

Ukadaulo Wauzimu:

Mlozo wa Nkhondo

Ya

Uzimu

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a Harvest International Institute ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinathandizira anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Nthcito Ka Bukuli.....	4
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	4
Mau Otsogolera.....	6
Zolinga Za Maphunzirowa.....	9

KUITANIDWA KU NKHONDO

1. Nkhondo Yosaoneka Ndi Maso.....	11
------------------------------------	----

Kulembedwa Usilikari

2. Kulowa Mu Gulu La Asilikari Ankhondo A Mulungu.....	22
--	----

Maphunziro Ofunika

3. Wankhondo Wamkulu: Ambuye Wa Makamu.....	33
4. Mphamvu Zauzimu Za Kuunika: Angelo	51
5. Mdani: Satana.....	63
6. Mphamvu Za Kumdima: Ziwanda.....	75
7. Dera La Mdani	84
8. Machenjeleri A Satana.....	95
9. Dongosolo La Mulungu Lo Menyera Nkhondo.....	101

KUKUSA

10. Nkhondi Yoipalamula Ndi Yodziteteza.....	125
11. Zida Zoyenera Nkhondo Yodziteteza.....	135
12. Zida Zomenyera Nkhondo Yoipalamula.....	146

13. Zinthu Zakuthupi Zofanana Ndi Nkhondo Yauzimu.....	154
--	-----

KUTHIRA NKHONDO

14. Kulowa Dera Lankhondo: Kulimbana Ndi Thupi, Dziko Ndi Satana.....	166
15. Nkhondo M'maganizo.....	183
16. Nkhondi Ya Lilime.....	199
17. Nkhondo Pa Malinga.....	216
18. Nkhondo Za Madera Ofunikira	226

MAPHUNZIRO A PAMWAMBA A NKHONDO YA UZIMU

19. Kupatsirana Mizimu.....	240
20. Choipa Muuzimu M'magome Am'mwamba.....	251
21. Kuthana Ndi Mphamvu Zoipa Ya Ziwanda.....	265
22. Okhudzidwa Ndi Nkhondo.....	293
23. Kugonja Pakumenyana Koma Ndikupambana Pa Nkhondo.....	310

KUFOTOKOZA KOMALIZA

24. Nkhondo Yomaliza.....	322
Zina Zapadera	332
Mayankho Akuyendera Perete	356

KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA BUKULI

KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

Zolinga: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Werengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

Vesi Yotsogolera: Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

Zopezeka mu Magawo: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

Mayeso Odziyesa Nokha: Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

Zophunzira Zowonjezera: Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mawu Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

Mayeso Omaliza: ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

ZOWERENGA ZINA ZOFUNIKA POPHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

MKUMANO WOYAMBA

Kutsekulira: Yambani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu: Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene muzikumana.

Mayamiko ndi Matamando: Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

Gawani Mabuku Kwa Ophunzira: Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

Perekani Ntchito Yoyamba. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene aziphunzitsidwa pa mkumano uli wonse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

Kutsekulira: Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina a ophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a ophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

Kukumbutsira: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

Phunziro: Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso m'mene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

Mayeso Odziyesa Nokha: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankho kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

Mayeso omaliza: Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

Phunziro: **Nkhonda Yauzimu:**

Mlozo wa Nkhondo Yauzimu

MAU OYAMBA

Pali nkhondo yaikulu imene ikumenyedwa pa dziko lapansi lero. Si nkhondo ya pakati pa maiko, mitundu, kapena atsogoleri a boma. Si gulu loukira boma. Ndi nkhondo yosaoneka ndi maso yomwe imachitika m'dziko lauzimu. Baibulo limanena kuti anthu a Mulungu amaonenga chifukwa cha kusadziwa (Hosea 4:6). Gawo limodzi limene anthu a Mulungu akuonongeka chifukwa cha kusadziwa ndiko kusowa chidziwitso pa nkhani ya nkhondo ya uzimu.

Mpingo woyamba umatenga utumiki ngati nkhondo yauzimu. Chilankhulo cha ku usilikari chagwiritsidwa ntchito m'Chipangano Chatsopano chonse. Chitetezo chimatengedwa ngati zida za Mulungu. Mau a Mulungu amayerkezedwa ndi lupanga. Mayesero a Satana amatchedwa mivi ya moto. Chikhulupiliro chinali nkhondo “kulimbana kwabwino” ndipo okhulupirira amauidwa kuti “alimbane kulimbana kwabwino.” Mpingo woyamba umadziwa kuti uli pa nkhondo yaikulu ya uzimu.

Nkhondo ya uzimuyi ikupitilirabe mpaka pano koma m'malo molimbana ndi mdani, okhulupirira atanganidwa ndikumanga matchalitchi akuluakulu, kugula zida zoimbira mu tchalitchi za mphamvu, kupanga maphwando, komanso kulimbana wina ndi mnzake mkatimkati mwa nkhondo yaikulu yauzimu yomwe ikuchitika mowazungulira. Satana waonjezera mphamvu pa kulimbana ndi mpingo womwe wachoka pa mzere wopenya nkhondo wa kutsogolo.

Pamene nthawi ya chimaliziro ikuyandikira nkofunika kwambiri kuti okhulupirira ayimvetse bwino nkhondo yauzimu kuposa omwe analipo m'mene mpingo umayamba. Paulo Mtumwi anachenjeza:

Koma zindikira ici, kuti masiku otsiriza zidzafika nthawi zowawitsa (2 Timoteo 3:1)

Kuti tikhale okonzekera bwino mu nthawi zowawitsa izi, tikuyenera kuonanso mwatsopano ndondomeko za nkhondo yauzimu. Moyo wa chikristu ndi nkhondo. Tikachita machawi kuzindikira ichi komanso kukonzekera bwino, tiona chigonjetso mwachangu.

“Koma pamene ukonza phwando uitane aumphawi, opunduka, otsimphina, akhungu” Luka 14:13

Palibe mfumu imene inalowa mu nkhondo ndi dziko lina isanayambe yafufuza kuthekera kwake komanso ukonza ndondomeko zabwino zomenyera nkhondo. Izitu ndi zomwe tikuchita m'phunziro ili. Tikupanga kafukufuku wosamalitsa bwino wa ndondomeko, zida ndi mphamvu zomwe tili nazo pamene tikulimbana ndi mdani wathu Satana.

Ku nkhondo akati “ndondomeko” ndi ukadaulo wokonza ndi kukwaniritsa njira za kamenyedwe ka nkhondo. Ndi njira yapaderadera yomwe imapangitsa kuti gulu lipambane pa nkhondo. Mu

phunziro lino, muphunzira kakonzedwe ndi kachitidwe ka ndondomeko ya nkondo yauzimu yomwe ikabweretsa chigonjetso mu dziko lauzimu.

BUKHU LINO

Phunziro liri lonse laperekedwa m'chilankhulo cha ku usilikari m'magawo ali m'musimu:

KUITANIDWA KU NKHONDO

Chaputala 1 chikufotokoza bwino nkondo yosaonekayi komanso kuliza lipenga la “maitanidwe a ku nkondo.”

KULEMBEDWA USILIKARI

Magulu onse a nkondo ali ndi njira zake zomwe limalemba asilikari ake. Izi ndi zinthu zapadera-dera zomwe munthu amayenera kuchita kuti alowe usilikari. Chimodzi-modzinso asilikari a Mulungu. Chaputala 2 chikufotokoza momwe mungalowere usilikari wauzimu.

MAPHUNZIRO OFUNIKA

Munthu akalowa usilikali amayenera alandire maphunziro. Tiona momwe Mulungu amaphunzitsira asilikali ake mu chaputala 3 ndi 9. Mizere ya nkondo yosaonekayi ikufotokozeredwanso bwino. Mphamvu zomwe zikulimbana pakati pa mtima ndi kuunika kuphatikizapo Ambuye wa Makamu, angelo, Satana, ziwanda, dziko lapansi komanso thupi. Dera la mdani komanso njira zake zazindikirika, komanso dongosolo la nkondo ya Mulungu laperekedwa.

KUKUSA

Maphunziro a usilikali atha kukhala opanda ntchito ngati asilikaliwo sakusidwa pamodzi. “Kukusa” kumatanthauza “kupanga gulu la nkondo kukhala lokonzeka kumenya nkondo.” Mu gawo la “Kukusa Gulu” m'phunziro lino mu chaputala 10 ndi 13, muphunzira kumenya nkondo moipalamula kapena modziteza; kagwiritsidwe ntchito ka zida za nkondo yano; ndi kufanana komwe kulipo pakati pa nkondo ya kuthupi ndi nkondo yauzimu.

KUTHIRA NKHONDO

Pokhathira nkondo (nkondo ya kuthupi) gulu la asilikali limakalowa m'dera la adani awo kukawagonjetsa ndi kulanda deralo. Maphunziro a usilikali atha kukhala opanda ntchito ngati zimene zaphunziridwazo sizigwiritsidwa ntchito. Ngakhale gulu la asilikali labweretsedwa pamodzi ndi kupatsidwa zida koma langoima chilili pambali poteropo zimakhala zopanda phindu. Kuti muchite bwino pa nkondoyi mukuyenera kulowa m'dera la mdani ndi kukathira nkondo. M'gawo la kuthira nkondo, zomwe zili mu chaputala 14 mpaka 19, mulowa m'dera la nkondo la dziko, thupi, ndi Satana. Muphunzira nkondo ya m'maganizo, ndi lilime, pamwamba pa zipupa za uzimu, malo okwera komanso m'madera ofunikira a nkondo. Mu

phunziro lili lonse tizindikira madongosolo a Satana pomenya nkhondo komanso tikambirana momwe tingam'gonjetsere.

MAPHUNZIRO A PAMWAMBA A NKHONDO YA UZIMU

Asilikali akalandira maphunziro oyambilira, amaphunzitsidwanso maphunziro ena a pamwamba m'magawo osiyana-siyana ofunikira a nkhondo. Ku usilikali, gulu lomwe lalandira maphunziro amenewa limatumidwa ku ntchito zovutirapo. M'gawo la "Maphunziro a Pamwamba a Nkhondo ya Uzimu" muphunzira kuyenderana kwa mizimu, m'mene mungathandizire am'ndende komanso ovulala pa nkhondo, kulimbana ndi mphavu za ziwanda. Muphunziranso za kuluza ndeu ndi kupambanabe nkhondo.

KUFOTOKOZA KOMALIZA

M'kufotokoza komaliza mu chaputala 26, muphunzira "kulimbana komaliza" komwe kudzabweretse nkhondo ya zakazakayi ku mapeto a chigonjetso.

GAWO LOMALIZA

Mu "Gawo Lomaliza" la buku lino, muona tsatane tsatane wa mbiri ya "Nkhondo Zikuluzikulu za m'Baibulo" pamene mukuchenusa maluso anu a nkhondo yauzimu.

MAPHUNZIRO

Phunziro lililonse m'buku lino lakonzedwa motere:

ZOLINGA

Izi ndi zolinga zapadera za nkhondo ya uzimu zomwe muyenera kukwaniritsa.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Pamene dziko likulengeza nkhondo, limayenera kutulutsa "Mfundo za Nkhondo". Izi zimafotokozerwa bwino chifukwa chimene akumenyera nkhondo, kutchula mdani, komanso kufotokozerwa zolinga za nkhondoyo. Baibulo ndi Mau olembedwa a Mulungu M'modzi Woona, Wamkulu wa nkhondo yathu ya uzimu. M'Baibulo ndi momwe timapeza Mfundo za Nkhondo yomwe tikumenya. M'phunziro lililonse "Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo" limatsindika ganizo lomwe likuperekedwa m'phunzirolo.

CHIYAMBI

Chiyambi chimapereka chithunzi-thunzi cha zomwe zili mu chaputala chimenecho.

PHUNZIRO

Gawo ili limapereka "kukumana kwa asilikali" mu chaputala chimenechi. Asilikali asananyamuke kunka ku nkhondo amayamba akumana kaye kulandira malangizo owathandiza kukamenya bwino nkhondo.

KUYENDERA

Ku nkhondo ya kuthupi, kuyendera kumachitika kawiri-kawiri kuti aone ngati kukonzekeretsedwa komanso maluso a asilikali. Gawo la “Kuyendera” m’chaputala chilichonse imaunika ngati mwakwaniritsa zolinga za phunziro limenelo.

MACHITA-CHITA OWONETSA LUSO

M’gawo ili asilikali amagwiritsa ntchito zomwe aphunzira mu nyengo ya nkhondo yeni-yeni. Gawo la machita-chita a luso limakupatsani mwayi wogwiritsa ntchito zomwe mwaphunzira ndi kuwerenga zinthu zina zolingana ndi phunziro limenelo.

MWAKONZEKA?

Kubweretsa poyera mdani ndi njira zake ndi limodzi mwa mabvumbulutso akuluakulu a Mau a Mulungu. Kwakukulu-kulu bvumbulutso lakuti ife monga okhulupilira tili ndi ulamuliro pa mphamvu zonse za mdani. Phunziro lino si mapeto a maphunziro onse a nkhondo yauzimu. Komabe ndi kafukufuku wozama kwambiri wa Malemba. Monga m’mene zimakhallira ku nkhondo yakuthupi, luso la nkhondo yauzimu limakhala likukula pang’ono-pang’ono pamene mukulowa m’dera la mdani kumenya nkhondo.

ZOLINGA

Mukamaliza maphunzirowa mukuyenera kukwanitsa:

- Kuzindikira maufumu awiri auzimu
- Kufotokoza tanthauzo la “nkondo yauzimu”
- Kuzindikira zomwe zimayambitsa kulimbana kwauzimu kwakukuru kotereku.
- Kuzindikira mphamvu zauzimu za kuunika
- Kuzindikira mphambu zauzimu za mdima
- Kuzindikira dongosolo la Satana
- Kugwiritsa ntchito bwino njira zogonjetsera za uzimu
- Kugwiritsa ntchito luso la nkondo ya kuthupi ku nkondo yauzimu
- Kugwiritsa ntchito zida zomenyera nkondo komanso zodzitetzera zauzimu.
- Kudziwa machitachita a ziwanda mwa munthu kapena chinthu china.
- Kumvetsa bwino momwe mamasulidwe ku ziwanda amapezekera
- Kupambana nkondo ngakhale mutalephera ndeu.
- Kufotokoza kulimbana komaliza komwe kudzathetsa nkondo yosaonekayi.
- Kuzindikira mfundo za nkondo yauzimu in nkondo zikulu-zikulu za m’Baibulo.

KUITANIDWA KU NKHONDO

KUITANIDWA KU NKHONDO YOSAONEKA

Pali nkhondo yaikulu yomwe ikumenyedwa pa dziko lapansi. Ndi nkhondo yomwe imachitika mwa munthu pakati pa thupi ndi mzimu. Ndi nkhondo yolimbana ndi mphamvu za kumdima pa dziko lapansi. Ndi nkhondo yolimbana ndi mphamvu zowopsa za ku mdima.

Mu nthawi za Chipangano Chakale lipenga limagwiritsidwa ntchito kuitanira anthu a Mulungu ku nkhondo. Lero kuitanidwa kwa uzimu kukumveka m' maiko onse a dziko lapansi. Uku ndiko kuitanidwa ku nkhondo yosaoneka. Ndi kuitanidwa ku nkhondo.

CHAPUTALA 1

NKHONDO YOSAONEKA NDI MASO

ZOLINGA

Pomaliza pa phunziro lino mukuyenera kukwanitsa kuchita izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kuonetsera kumvetsa bwino zinthu za kuthupi komanso za ku kuuzimu
- Kumasulira mau oti “mfumu.”
- Kumasulira mau oti “ufumu.”
- Kuzindikira maufumu awiri a muuzimu.
- Kupeza ufumu womwe inu muli.
- Kuzindikira mphamvu za kumdimba
- Kuzindikira mphamvu za kukunika
- Kufotokozera bwino tanthauzo la mau oti “nkhondo yauzimu.”
- Kudziwa zifukwa zomenyera nkhondo yosaoneka
- Kudziwa mfundo zoyambilira pa kumvetsa bwino za nkhondo yauzimu.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO:

Aefeso 6:12 Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba.

MAU OYAMBA

Monga mwaphunzira kale kumayambiro a phunziro lino, pali nkhondo yaikulu yomwe ikumenyedwa pa dziko lapansi lero. Si kulimbana kwa pakati pa maiko, mitundu kapena atsogolera a maboma. Si kuukira kapena kulanda boma. Ndi nkhondo yosaoneka yomwe ikuchitika mu dziko lauzimu.

Chaputala chino chikutengera ku nkhondo yosaoneka yomwe wokhulupirira aliyense akumenya. Ndi nkhondo yomwe palibe amene amavala unifolomu komanso imakhudza aliyense. Mbiri komanso uneneri wokhuza nkhondo imeneyi zimapezeka m’Baibulo, Mau a Mulungu.

DZIKO LA KUTHUPI NDI DZIKO LA KUUZIMU

Kuti mumvetse bwino za nkhondo yosaonekayi, mukuyenera kumvetsa bwino za dziko la kuthupi komanso dziko lauzimu. Munthu amakhala m’maiko awiri: Dziko la kuthupi ndi dziko la kuuzimu. Dziko lauzimu ndi lomwe limaoneka, kumveka, kukhudzika, ndi kulawika. Ndi dziko logwirika komanso lowoneka ndi maso. Dziko, boma, mudzi womwe mukukhala uli mbali imodzi ya dziko la kuthupi. Ndi mzika wa mu ufumu wa dziko la kuthupi lomwe likupezeka

mdera la maiko a m'dziko. Mumatha kumaona anthu ali mdera lanu. Mumalankhula nawo. Mumaona zomwe zili m'dera lanu, kumva phokoso komanso fungo lokuzungulirani.

Kulinso dziko lina lomwe inu m'makhalako. Dziko limeneli ndi dziko lauzimu. Simungathe kuona dzikoli ndi maso anu a kuthupi, koma lilipo ndithu monga momwe liliri dziko la kuthupi lomwe mumakhala. Paulo akulankhula za kusiyana kwa mbali ziwirizi:

1 Akorinto 15:10 Koma ndi cisomo ca Mulungu ndiri ine amene ndiri; ndipo cisomo cace ca kwa ine sicinakhala copanda pace, koma ndinagwirira nchito yocuruka ya iwo onse; koma si ine, komacisomo ca Mulungu cakukhala ndi ine.

Anthu onse ali ndi thupi lomwe limakhala m'dziko la kuthupi, koma munthu alinso muuzimu wokhala ndi moyo ndi mzimu zokhala ku nthawi ndi nthawi. Munthu ali ndi thupi, moyo ndi mzimu. Gawo lanu la uzimu (moyo ndi mzimu) ndi mbali dziko la uzimu ndipo thupi lanu ndi gawo la dziko la kuthupi.

KUZINDIKIRA KWA MUUZIMU

Popeza kuti nkondo yauzimu imachitika muuzimu, ikuyeneranso kumvetsetsedwa ndi ganizo lauzimu. Mu nzeru zathu za kuthupi ndi zolepherazi sitingamvetse bwino zinthu za uzimu.

1 Akorinto 2:14 Koma munthu wa cibandwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu.

Nkoyenera kugwiritsa ntchito kuzindikira kwa muuzimu kuti tikamvetse zinthu za uzimu.

Mwina chitsanzo chabwino cha kuzindikira zinthu muuzimu chikupezeka pa 2 Mafumu 6. Pali nkhani ya nkondo ya kuthupi m'mene asilikali a dziko la Asuri lomwe linali pa udani Israel linazungulira kamudzi kakang'ono kotchedwa Dotani komwe Mneneri Elisa anali kukhala. Pamene Gehazi, mnyamata wa Elisa, anaona gulu lalikulu la asilikali a Asuri, anachita mantha. Koma Elisa anapemphera kuti Mulungu atsegule maso a uzimu a Gehazi kuti aone gulu la angelo lomwe linawazungulira komanso kuwateteza iwo. Apatu Mulungu anatsegula maso a kuthupi a Gehazi ndi kumuonetsa asilikali a Mulungu ochuluka omwe anaima kuti amenye nkondo.

Nkhani ya nkondo ya ku Dotaniyi ikufanana ndi nyengo zauzimu za Mpingo wa lero. Pali ena, okhala ngati Elisa, omwe amaona bwino zochitika m'dziko la uzimu. Amadziwa za kulimbana komwe kulipo, anamzindikira mdani komanso amazindikira mphamvu yoopsa ya Mulungu yomwe imatitsimikizira za chigonjetso. Koma pali ena, ngati Gehazi, omwe ndi chilimbikitso chochepa atha kutsegula maso awo ndipo sadzachitanso mantha ndipo sadzagonjetsedwa ndi mdani. Mwa tsoka, kulinso anthu ena omwe ali ngati aja okhala mdziko la Dotani, amene akugona muuzimu. Sazindikira konse kuti mdani wawazungulira ndipo wakonzeka kumenya nkondo.

MAUFUMU AWIRI AUZIMU

Mbali ya kuthupi komanso kuuzimu yomwe tikukambayi ili ndi mafumu awiri osiyana omwe akulamulira ndi atsogoleri a kuthupi ndinso kuuzimu.

MAUFUMU A KUTHUPI

Anthu onse amakhala mu ufumu wa kuthupi wa dziko lino. Akukhala m'mudzi kapena mzinda womwe uli mbali imodzi ya dziko lina lake. Dziko limenelo ndi ufumu wa dziko lapansi. Ufumu mdziko lino lapansi ndi dera kapena anthu omwe mfumu yeni-yeni imalamulira. M'Baibulo maufumuwa amatchedwa “maufumu a dziko lapansi.” Maufumu a dziko lapansi amabwera pansu pa mphamvu ndi machita-chita a Satana:

Pomwense mdierekezi anamuka naye ku phiri lalitari, namuonetsa maiko onse a dziko lapansi, ndi ulemerero wao; nati kwa Iye, Zonse ndikupatsani Inu, ngati mudzagwa pansu ndi kundigwadira ine. (Mateyu 4:8-9)

amatikumbutsa kuti “dziko lapansi liri pansu pa ulamuliro wa woipayo.” (Yohane 5:19)

MAUFUMU A KUUZIMU

Kuonjezera pa maufumu a dziko lino lapansi, kulinso maufumu awiri muuzimu: Ufumu wa Satana ndi Ufumu wa Mulungu. Munthu aliyense wamoyo amakhala mu ufumu umodzi mwa mafumu awiriwa.

Mu Ufumu wa Satana muli Satanayo, ziwanda ndi anthu onse okhala mu uchimo ndi kugalukira kwa Mau a Mulungu. Zinthu izi pamodzi ndi dziko komanso thupi ndizo mphamvu za kumdima zomwe zikugwira ntchito pa dziko lapansi lero.

Mu Ufumu wa Mulungu muli Mulungu Atate, Yesu Khristu, Mzimu Woyera angelo ndi anthu onse omwe amanvera Mau a Mulungu mwa chilungamo. Izi ndizo mphamvu za kuunika.

Ufumu wa Mulungu si mpingo ayi. Mipingo ndi mabungwe kapena magulu opangidwa ndi anthu. Anakhazikitsidwa kuti pakhale dongosolo m'machitidwe a zinthu. Tikati mpingo tikukamba za magulu monga Baptist, Assembly of God, Methodist, Lutheran ndi ina yambiri. Baibulo limakambanso za mpingo womwe suli ngati mipingo kapena magulu a chipembedzo omwe tatchulawa. Mpingo weni-weni umapangidwa ndi omwe ali mzika za Ufumu wa Mulungu.

Ku dziko la kuthupi panopa, Ufumu wa Mulungu umachitika mkati mwa mtima wa munthu payekha-payekha, wamwamuna, wamkazi, mnyamata kapena mtsikana yemwe wampanga Yesu kukhala Mfumu ya moyo wake. Umachitikanso m'gulu la anthu pa mpingo komanso paliponse pomwe pakuchitika zomwe Mulungu amafuna. Mtsogolomu mudzakhala ufumu weni-weni woonetsera Ufumu wa Mulungu.

NKHONDO YOSAONEKA

Nkhondo yosaoneka yauzimu ndi nkhondo yomwe imakhudza amuna ndi akazi onse. Chifukwa chakuti Ufumu wa Satana ndi ufumu wauzimu:

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

Nkhondo yauzimu si nkhondo ya kuthupi pakati pa thupi ndi mwazi ayi. Si nkhondo ya pakati pa munthu ndi munthu mzake ayi. Si nkhondo yooneka ndi maso ayi. Koma ndi kulimbana kosaoneka m'dziko la uzimu. Ndi nkhondo yochitika mkati komanso mozungulira munthu. Ndi nkhondo yosaoneka chifukwa imachitika ndi mizimu ndipo timaphunzira pa Luka 24:39 kuti mizimu ulibe mnofu ndi mafupa.

Nkhondo yauzimu imachitika “m'magawo a mitundu-mitundu,” kutanthauza kuti imamenyedwa m'magawo osiyana-siyana. Iyi ndi:

1. Nkhondo ya makhalidwe yolimbana pakati pa wokhulupirira ndi dziko: Yohane 15:18-27.
2. Nkhondo ya munthu payekha yolimbana pakati pa tnupi ndi mzimu: Agalatiya 5:16-26.
3. Nkhondo ya yoopsa yolimbana pakati pa okhulupirira ndi mphamvu zoipa za kumdima: Aefeso 6:10-27.

Munthu aliyense wa moyo amamenya nawo nkhondoyi kaya akuzindikira kapena ayi. Palibe ali chikati-kati. Osakhulupirira ali mu nsinga ku zoipa ndipo atengedwa kukhala akapolo a mphamvu za mdaniyo. Iwo akunka aowonongeka mu nkhondoyi.

Okhulupirira anaombedwa ku mphamvu ya mdani mwa Khristu Yesu ndipo ali agonjetsi koma akumenyabe nkhondoyi. Mu vesi lathu lotsogolera mu chaputala chino likuonetsa kuti ife (tonse okhulupirira) tikulimbana ndi mphamvu za kumdima.

Tikati “kulimbana” ndiye kuti pali kugwira mthupi. Palibe amene sakuchita nawo nkhondoyi. Palibe amene amaionera patali. Muli pakati-kati pa kulimbana kaya mukudziwa kapena ayi. Ngati mukuona kuti nkhondo ikhala ikuchepa pang'ono-pang'ono, mwalemba m'madzi. Nkhondo yauzimu siimatha.

KOMWE NKHONDOYI IMACHITIKIRA

Nkhondo yosaonekayi imachitika pa dziko lapansi:

Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)

Satana amakhala akumenya nkhondo ndi cholinga chofuna kukhalabe wolamulira maufumu a dziko lapansi. Safuna kuti anthu akhale pansu pa ulamuliro wa Mulungu. Nkhondoyi

imachitikanso m'mitima, m'malingiliro komanso m'miyoyo ya amuna ndi akazi. Satana amaphimba maso a osakhulupirira komanso kulimbana ndi okhulupirira m'magawo a kulambira Mulungu, m'Mau, mu ubale wao ndi Mulungu komanso mu utumiki wao.

MOMWE NKHONDOYI IDAYAMBIKIRA

Nkhondo yosaonekayi idayambira Kumwamba ndi m'ngelo wotchedwa Lucifala yemwe anali m'ngelo wokongola kwambiri wolengedwa ndi Mulungu ndipo anali gawo limodzi la Ufumu wa Mulungu. Mutha kuwerenga za kuwukiraku pa Yesaya 14:12-17 ndi Ezekiel 28:12-19. Muphunzira zambiri za izi patsogolopa m'maphunziro omwewa. Kagulu ka angelo kanamlondola Lucifa (tsopano wotchedwa) nkuukiraku. Lucifa ndi kagulu konse koukira ka angelo kanachotsedwa kumwamba ndi Mulungu. Iwo anapanga ufumu wawo-wawo padziko lapansi:

Ndipo munali nkhondo m'mwamba. Mikayeli ndi angelo ace akucita nkhondo ndi cinjoka; cinjokanso ndi angelo ace cinacita nkhondo; (Cibvumbulutso 12:7)

Ndipo cinaponyedwa pansu cinjoka cacikuru, njoka (Cibvumbulutso 12:9) yokalambayo, iye wochedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse; cinaponyedwa pansu kudziko, ndi angelo ace anaponyedwa naye pamodzi.

Lucifa anayamba kutchedwa Satana ndipo angelowo anatchedwa ziwanda. Mizimu ya ziwanda imatha kulowa, kuzunza, kulamalira komanso kugwiritsa ntchito munthu amene ali wa mu Ufumu wa Satana. Amalimbikitsa ntchito zoipa zochitika ndi amuna ndi akazi omwe. Satana amalamalira ziwanda zake kuti zikhale patsogolo mu zochita zawo zoipazo. Amaphatikiza mphamvu zoopsa zimenezi ndi dziko komanso thupi kuchita nkhondo pakati pa mtundu wa anthu.

ZIFUKWA ZOPANGITSA KUTI KULIMBANA KUKHALEPO

Munthu poyambayamba analengedwa mchifanizo cha Mulungu ku ulemelero wake (Genesesi 2). Nkhondo yosaoneka yolimbana ndi munthu inayambika ndi yesero m'munda wa Genetsemani (Genesesi 3). Satana anapangitsa kuti Adamu ndi Hava achimwe. Izi zinapangangitse anthu onse obadwa kuchoka mwa Adamu kuti akhale ndi chikhalidwe cha uchimo ndi kuyamba kuchita machimo:

Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa ucimo; coteru imfa inafikira anthu onse, cifukwa kuti onse anacimwa. (Aroma 5:12)

Zinapangitsanso kuti pakhale nkhondo yosaoneka pakati pa munthu ndi mphamvu za kumdima.

ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace. (Genesis 3:15)

Chifukwa cha uchimo munthu anasiyanitsidwa ndi Mulungu naweruzidwa ndi imfa. Koma Mulungu anamkonda munthu koposa nam pangira dongosolo lakuti apulumutsidwe ku uchimo:

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi iye. (Yohane 3:16-17)

Kudzera m'chikhulupiriro mwa Yesu, kuvomereza ndi kulapa machimo, amuna ndi abambo angathe kumasulidwa ku mphamvu ya mdani. Imfa ndi chiukitso cha Yesu sizinangotibweretsera chipulumutso ku uchimo. Zinagonjetsanso mdani, Satana:

iye wocita cimo ali wocokera mwa mdierekezi, cifukwa mdierekezi amacimwa kuyambira paciyanbi. Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge nchito za mdierekezi, (1 Yohane 3:8)

Ngati Satana anagonjetsedwa, nchifukwa chiani nanga pali kulimbana kwakukuru kotere? Pa nkondo ngakhale adani agonjetsedwe, safuna kuvomereza mpakana atakamizidwa kutero. Ngakhale Yesu anagonjetsa Satana, tikukhala mdera lomwe likadali m'manja mwa mdani wosafuna kuvomereza. Kumvetsa bwino ndondomeko za nkondo yauzimu kumatipatsa kuthekera kolimbana ndi mphamvu za kumdimazi.

Satana akuyesayesa kupanga anthu kuti akhalebe mu ukapolo wa tchimo. Kudzera mu njira zonyenga akukopa amuna ndi abambo ku zisiliro zoipa ndi moyo wauchimo. Amafuna atamalamulira moyo ndi mzimu wa munthu zomwe ndi za Mulungu.

Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)

Satana amafuna atakhalabe wolamulira wamkulu. Akumenya nkondo yolimba pofuna kutenga ulamuliro pa mtima, maganizo, moyo ndi mzimu wa munthu. Akulimbana ndi Mulungu, dongosolo lake komanso anthu ake. Nkhondoyi ipitilirabe kufikira kulimbana kwakukuru komwe muphunzire mu chaputala chomaliza.

TANTHAUZO LA NKHONDO YAUZIMU

Nkhondo yauzimu ndi kafukufuku komanso kutengapo mbali pomenya nkondo yosaoneka yauzimu. Timasanthula mphamvu zotsutsana za kuunika ndi mdima, ndondomeko za Satana, ndi ndondomeko zauzimu zothana ndi mphamvu ya mdani. Nkhondo yauzimu imaposa kungochita kafukufuku wa mfundo zauzimu. Imafunanso kutenga mbali kwakukuru pogwiritsa ntchito ndondomeko zimenezi m'moyo ndi mu utumiki wathu.

Njira imodzi yomwe amagwiritsa ntchito kwambiri ndiyo kupanga okhulupirira kukhala osadziwa za dongosolo lake. Paulo analankhula kuti nkofunika kudziwa machenjerero a Satana:

**kuti asaticenierere Satana; pakuti sitikhala osadziwa macenjerero ace.
(2 Akorinto 2:11)**

Tikuyenera kuphunzira momwe tingathere njira zomwe Satana amagwiritsa ntchito polimbana ndi okhulupirira. Tikuyeneranso kumvetsa bwino zomwe Malemba akunena zokhuza chigonjetso chomwe tili nacho pa Satana ndi mphamvu za kumdima. Taitanidwa kukamenya nkondo mwa luso. Kuti munthu amvetse bwino za nkondo yauzimu asunge mfundo iyi:

Munthu akuyenera kudziwa kuti nkondo zonse m'moyo uno, kaya kuthupi, muuzimu, m'maganizo, zachuma kapena makhalidwe a umunthu zimakhala kuonetsera chabe kwa zomwe zikuchitika m'dziko lauzimu.

Ngakhale mavuto amatha kubwera chifukwa cha zochitika chitika m'moyo uno, kuseli kwa zonsezi kumakhala nkondo yauzimu yomwe ikuchitika.

Tayesera kukonza mavuto a dziko lino kudzera m'maphunziro, malamulo, ndi kusamalira malo okhala. Zonsezi sizinaphule kanthu chifukwa mavutowa ndi zotsatira za nkondo yauzimu yomwe ikuchitika mkatikati. Sangathetsedwe ndi nzeru za umunthu.

KODI NDINU A MU UFUMU UTI?

Kuthupi mfumu ndiye wolamulira wamkulu wa ufumu. Dera lonse pamodzi ndi anthu omwe amakhala kuti ndizake. Ali ndi mphamvu pa moyo ndi imfa za omwe akuwalamulira. Chimodzimodzinso mu ufumu wauzimu. Mwina muli mbali ya Ufumu wa Mulungu kapena Ufumu wa Satana. Moyo wanu umalamuliridwa ndi Mulungu kapena Satana.

Limodzi mwa mafanizo omwe Yesu anauza ophunzira ake likuonetsa kuti anthu amakhala ndi mbali yomwe ali, ya Ufumu wa Mulungu kapena wa Satana. Yesu anayerekeza dziko lapansi ngati munda. Mbeu yabwino m'munda muja ndi ana a mu Ufumu wa Mulungu. Mbeu yoipa yomwe inabala minga ndi ana a woipayo.

Mateyu 13:38 ndipo munda ndiwo dziko lapansi; ndi mbeu yabwino ndiyo ana a Ufumuwo; ndi namsongole ndiye ana a woipayo;

Anthu amalowa mu Ufumu wa Satana kudzera nkubadwa. Baibulo limaphunzitsa kuti anthu onse amabadwa mu uchimo. Kutanthauza kuti mwa iwo muli chikhalidwe cha uchimo kapena mbeu ya uchimo. Akangobadwa, chikhalidwe cha uchimo chimayambiratu kuonekera.

**Onani, ndinabadwa m'mphulupulu: Ndipo mai wanga anandilandira m'zoipa.
(Masalmo 51:5)**

pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemmerero wa Mulungu; (Aroma 3:23)

Popeza kuti timabadwa ndi chikhalidwe chauchimo, ndiye kuti wina aliyense wa ife anakhalako wa mu Ufumu wa Satana. Iwo amene adakali mu uchimo ndi a mu Ufumu wa Satana mpaka pano.

Uthenga wa Mau a Mulungu olembedwa, Bukhu Lopatulika, ndi womema anthu kuti achoke mu Ufumu wa Satana kulowa mu Ufumu wa Mulungu. Anthu amabadwira mu Ufumu wa Satana pobadwa kuthupi. Akuyenera kubadwira mu Ufumu wa Mulungu pobadwanso mwauzimu. Chiphaso cholowera mu Ufumu wa Mulungu ndikubadwa mwatsopano basi monga m'mene afotokozera pa Yohane 3.

M'nkhondo yosaonekayi muli magawo awiri. Yesu anati, "Iye amene sali ndi ine ali wotsutsana nane." (Luka 11:12). Simungakhale opanda mbali mu nkhondo iyi. Muli iyi kapena inayo. Okhulupirira ena, chifukwa chosalimba mtima kutsutsana ndi mdani, salabadira za nkhondoyi ndi kukhala pa tchuti chomenya nkhondo. Amaganiza kuti ngati samlabadira mdaniyo iyeyo sawavutanso konse. Iyi ndi njiranso ina imene Satana amagwiritsa ntchito. Amayeseses kuopseza asilikali a Mulungu ndi zoopseza zake pofuna kuti iwo asataketakenso.

Palibe anganene kuti alibe mbali. Muli mbali yogonjetsedwa kapena yogonjetsa. Maitanidwe a ku nkhondo akumveka. Kodi muli mbali ya kuunika kapena yamdima? Kodi muli mbali ya Ufumu wa Mulungu kapena wa Satana? Kodi ndinu a ufumu uti? Kodi mu nkhondo yosaonekayi, ndinu wogonjetsedwa kapena wogonjetsa?

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Kodi ndi magawo ati amene aikidwa molingana ndi 1 Akorinto 15:44-49?

3. Kodi ndi maufumu ati osaoneka m'dzikoli lero?

4. Lembani m'ndandanda wa mphamvu za mdima.

5. Lembani m'ndandanda wa mphamvu za kuunika.

6. Tanthauzirani mau oti “mfumu.”

7. Tanthauzirani mau oti “ufumu.”

8. Kodi mau oti “nkhondo yauzimu” amatanthauza chiani?

9. Kodi nchifukwa chiani pali kulimbana kwauzimu kwakukuru kotere?

10. Kodi mfundo yofunika kwambiri pakumvetsa bwino za nkhondo yauzimu ndi yotani?

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto a buku lino).

MACHITA-CHITA A LUSO

1. Maphunziro ano, “Ndondomeko za Nkhondo Yauzimu,” imalunjika ku Ufumu wa Satana komanso nkhondo yauzimu yomwe imachitika pakati pa ufumu wake ndi Ufumu wa Mulungu. Phunziro la Harvestime International Institute yotchedwa “Kukhala Moyo wa mu Ufumu” limasanthula bwino za Ufumu wa Mulungu. (Ngati mukuchita maphunziro a Harvestime International Institute mu ndondomeko yake ndiye kuti mwaphunzira kale zimenezi.) Ngati siinu wophunzira wa Harvestime Institute, mukuyenera mupeze buku la “Kukhala Moyo wa mu Ufumu” popeza zimayendera limodzi ndi phunziro lino. Nzofunika kuti mumvetse bwino za maufumu onse awiri omwe akugwira ntchito m’dziko lapansi lero.
2. Kukhala ndi maziko abwino auzimu nkofunika kuti mukamenye bwino nkhondo yauzimuyi. Ngati mwangolandira kumene Yesu, pezani phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa, “Maziko a Chikhulupiro.” (Koma ngati mukupanga maphunziro a Harvestime mu ndondomeko yake ndiye kuti mwaphunzira kale za Maziko a Chikhulupiro).
3. Kodi mukuona kuti mwakhala wogonjetsedwa mu nkhondo yauzimuyi? Kodi ndi gawo liti la moyo kapena utumiki wanu limene mukuona kuti mukugonjetsedwa? Kodi ndi gawo la zachuma, lamaganizo, lakuthupi, lauzimu, ndi makhaliidwe a umunthu? Nkwabwino kuzindikira madera amene mukugonjetsedwa ndi cholinga chakuti mugwiritse bwino ntchito chidziwitsochi moyenera m’magawo amenewo.
4. Onaninso nkhanu ya pa 2 Mafumu 6 yomwe yakambidwa kale mu phunziroli. Kodi mukudziwa anthu ena omwe ali ngati Gehazi kapena ngati aja anali mu mzinda wa Dotani? Kodi mungawathandize motani?
5. Popeza kuti nkhoodoyi ili m’magawo ambiri, tikuyenera kulimbana ndi uchimo mwa ife, mphamvu za mdima m’dziko ndi mphamvu zoopsa ndi utumiki wa mamasulidwe.
6. Werengani Baibulo monga ngati buku la nkhondo yauzimu. Ndi mbiri ya momwe nkhondo yauzimu, kuonetsera kugonjetsa ndi kugonjetsedwa komwe kwakhala kulipo m’nkhoodo zam’mbuyomu. Ndi buku la uneneri wa momwe nkhondo yathu ikuyendera kufikira kulimbana kotsiriza.

KULOWA USILIKARI

KUKHALA M'MODZI WA ASILIKARI A MULUNGU

Magulu onse ankhondo padziko lapansi ali ndondomeko zomwe amatsata polemba anthu usilikali... zinthu zomwe munthu ayenera kukwaniritsa kuti akhala msilikali wa nkhondo.

Mwakonzeka kukhala gawo limodzi la gulu la asilikali a Mulungu?

CHAPUTALA 2

KULOWA MU GULU LA ASILIKALI A NKHONDO A MULUNGU

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputala chino mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kumasulira mau oti “kulapa.”
- Kufotokoza kufunika kwa kulapa.
- Kumasulira “kutembenuka mtima”
- Kufotokoza kufunika kwa kutembenuka mtima
- Kumasulira mau oti “kulungamitsidwa.”
- Kufotokoza tanthauzo la “kupulumutsidwa.”
- Kugwiritsa ntchito fanizo la Mwana Wolowelera pofotokoza kulapa ndi kutembenuka mtima.

VESI LA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Koma Yesu anadziwa zoyesayesa zao, nayankha, nati kwa iwo, Muyesayesa bwanji m'mitima yanu? (Luka 5:22)

MAU OYAMBA

Mu chaputala changothachi mwaphunzira za nkhondo yosaoneka yaikulu mdziko lauzimu. Mu chaputala chino muphunzira momwe mungalowele mu gulu la asilikali a nkhondo a Mulungu. Ku dziko kuno asilikali ali ndi miyambo yapadera yomwe amatsata kuti munthu afike poti walowa usilikali. Mwambowu umampanga kulowa nawo usilikali.

Mulungu ali ndi dongosolo lapadera lolowetsera asilikali ngati munthu akufuna kukhala m'modzi mwa asilikali ake. Dongosolo lake lagonera pa mfundo ziwiri zofunika kwambiri, kulapa ndi kutembenuka mtima komwe kumabweretsa kulungamitsidwa.

KULAPA

Kudziko kuno, munthu akalowa usilikali, akuyenera kulumbira kusiya kudzipereka kwake ku dziko lina kapena ku gulu lina la nkhondo. Ukalowa mu gulu la asilikali a Mulungu, ukuyenera kulapa kudzipereka kwako ku uchimo ndi ku Ufumu wa Satana. Izi zimachitika kudzera nkulapa.

Kulapa ndi “chisankho cha mkati kapena kusintha kwa maganizo komwe kumadzaonekera kunja potembenuka kuchoka ku uchimo kuloza kwa Mulungu ndi chilungamo.” Machitidwe 20:21 amakutchula kuti “kulapira kwa Mulungu.” Pongolapa pokhapo munthu umatembenuka kuchoka ku uchimo komanso ku Ufumu wa Satana.

Kulapa ndi chisankho chomwe munthu amapanga payekha kusintha kudzipereka kwake kuchokera ku Ufumu wa Satana kupita ku Ufumu wa Mulungu. Kusintha kwa maganizo ndi kutembenuka kuchoka ku uchimo kotereku sikungachitike ndi munthu payekha. Ndi mphamvu ya Mulungu yomwe imabweretsa kusintha m'maganizo, mumtima komanso m'moyo wa wochimwa: 1001469847

Ndipo pamene anamva izi, anakhala du, nalemekeza Mulungu, ndi kunena, a Potero Mulungu anapatsa kwa amitundunso kutembenukira mtima kumoyo. (Macitidwe 11:18)

Kulapa ndi mphatso ya Mulungu:

Ameneyo Mulungu anamkweza ndi dzanja lace lamanja, akhale Mtsogoleri ndi Mpulumutsi, kuti apatse kwa Israyeli kulapa, ndi cikhululukiro ca macimo. (Macitidwe 5:31)

Ngakhale zomvaimva mu mtima zimakhhalapo pamene munthu akulapa, kulapa kweni-kweni ndi chisankho, osati zongomva m'moyo. Kumva chisoni chifukwa cha uchimo ndi kukhetsa misonzi ndi zosakwanira mwa zokha. Zikuyenera ziyendere pamodzi ndi chisankho cha mkati chomwe chimabweretsa kusintha koonekera kunjira.

KUFUNIKA KOLAPA

Kulapa ndi kofunika chifukwa:

Mulungu amakulamulira:

...koma tsopano akulamulira anthu konse konse kuti atembenuke mtima (Machitidwe17:30).

Nkofunika kuti munthu apewe Imfa Yauzimu:

Ndinena kwa inu, iaitu; koma ngati inu simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse momwemo. (Luka 13:3)

Nkofunika kuti munthu apeze moyo wosatha:

Kudzera nkulapa chilango cha imfa chimachotsedwa ndipo moyo wosatha umaperekedwa:

Koma ndinati, Iaitu, Ambuye; pakuti kanthu wamba, kapena konyansa sikanalowe m'kamwa mwanga ndi kale lonse. (Macitidwe 11:8)

Nkofunika kuti munthu alandire chikhululukiro:

Mulungu sangakhululukire machimo anu pokha-pokha mutalapa:

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku chikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. (Macitidwe 2:38)

Ndi chikhumbo-khumbo cha Mulungu kwa onse:

Mulungu safuna munthu wina akaone imfa yauzimu yokusiyanitsidwa ndi Mulungu ku nthawi za nthawi m'Gahena:

Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. (2 Petro 3:9)

Ndi chifukwa chomwe Yesu anabwelera ku dziko lapansi:

Sindinabwelera olungama koma ochimwa kuti akalape (Luka 5:32).

Nkofunika kuti munthu akalowe mu Ufumu wa Mulungu:

Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kulalikira, ndi kunena, Tembenukani mitima, pakuti Ufumu wa Kumwamba wayandikira. (Mateyu 4:17)

Munthu akakhala mbali imodzi ya Ufumu wa Mulungu ndiye kuti walowa mu gulu la asilikali a Mulungu.

KUTEMBENUKA MTIMA

Munthu akapempha chikhululukiro cha machimo amapeza “kutembenuka mtima.” Kutembenuka mtima kumatanthauza “kutembenuka.” Mau awa akagwiritsidwa ntchito molumikizana ndi kulapa kwa m'Baibulo amatanthauza “kutembenuka kuchoka ku njira yoipa kunka ku njira yabwino.” Umachoka mu Ufumu wa Satana umalowa mu Ufumu wa Mulungu.

Ndipo iye adzatembenezira ana a Israyeli ambiri kwa Ambuye Mulungu wao. (Luka 1:16)

Ndipo anamuona iye onse akukhala ku Luda ndi ku Saron, natembenukira kwa Ambuye amenewa. (Macitidwe 9:35)

Ndipo dzanja la Ambuye linali nao; ndi unyinjira wakukhulupira unatembenukira kwa Ambuye. (Macitidwe 11:21)

Kutembenuka mtima kumatanthauza kutembenuka kuchoka ku mdima wa uchimo kuloza ku kuwala kwa chilungamo cha Mulungu:

Kuwatembenuka kuchoka ku mdima kunka kukuunika (Machitidwe 26:18).

Ndi kutembenuka kuchoka ku mphamvu ya Satana kupita kwa Mulungu:

Kuwatembenuza...kuchoka ku mphamvu ya Satana kunka kwa Mulungu (Machitidwe 26:18).

Ndi kutembenuka kuchoka ku zinthu za dziko lapansi kunka ku zinthu za uzimu:

napfuula Dati, Anthuni, bwanji mucita zimenezi? ifenso tiri anthu a mkhalidwe wathu umodzimidzi ndi wanu, akulalikira kwa inu Uthenga Wabwino, wakuti musiye zinthu zacabe izi, nimutembenukire kwa Mulungu wamoyo, amene analenga zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zonse ziri momwemo: (Macitidwe 14:15)

Ndi kutembenuka kuchoka ku milungu yonama kunka kuloza kwa Mulungu Wooni ndi Wamoyo:

Pakuti iwo okha alalikira za ife, malowedwe athu a kwa inu anali otani; ndi kuti munatembenukire kwa Mulungu posiyana nao mafano, kutumikira Mulungu weni weni wamoyo, (1 Atesalonika 1:9)

KUFUNIKA KWA KUTEMBENUKA MTIMA

Kutembenuka mtima kumayenera kuyendera pamodzi ndi kulapa. Munthu amayenera kutembenuka kuchoka ku zoipa kunka ku zabwino chifukwa....

Nkofunikira polowa mu Ufumu wa Mulungu:

nati, Indetu ndinena kwa inu, Ngati simutembenuka, nimukhala monga tianato, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 18:3)

Kumapululumutsa ku Imfa Yauzimu

azindikire, kuti iyeamene abweza wocimwa ku njira yace yosocera adzapulumutsa munthu kwa imfa, ndipo adzabvundikira macimo aunyinji. (Yakobo 5:20)

Nkofunika pofufuta machimo:

Machimo anu alembedwa m'buku la Mulungu kufikira tsiku lomwe mudzalape ndi kutembenuka, pamenepo machimo anu amafufutidwa: s

Cifukwa cace lapani, bwererani kuti afafanizidwe macimo anu, kotero kuti zidze nyengo zakutsitsimutsa zocokera ku nkhope ya Ambuye; (Macitidwe 3:19)

MWANA WOLOWELERA

Kulapa ndi kutembenuka zafotokozeredwa bwino kwambiri mu fanizo la Mwana Wolowelera. Werengani nkhani ya pa Luka 15:11-24. Mnyamata uyu anachoka kwa bambo ake ndi kunyumba kwake kupita ku dziko lakutali ndipo kudzera m'moyo wachitaiko anasakaza zonse zomwe anali nazo. Kumapeto kwake iye anzindikira za vuto lake. Anali wa njala, wosungulumwa, wausiwa, nagwira ntchito yoweta nkhumba. Kenako anapanga chisankho chofunika kwambiri. Iye anati,

“Ndinyamuka ndipita kwa bambo anga.” Chisankho chamkati ichi chinabweretsa kusintha koonekera kunjira. Anapita kwawo kukapempha chikhululukiro kwa bambo ake.

KULAPA... KUSINTHA KWA MAGANIZO

Werengani Luka 15:17-19. Mnyamatayu anazindikira za moyo wake wa uchimo. Anapanga chiganizo chopita kwa bambo ake ndi kulapa tchimo lake. Ichi ndi chitsanzo cha kulapa, chiganizo cha mkati chobweretsa kusintha m’machitidwe a zinthu.

KUTEMBENUKA MTIMA.... KUCHITAPO KANTHU PA CHIGANIZO

Luka 15:20 imafotokoza momwe mnyamatayu anadzukira kusiya moyo wakale ndi kupita kwa bambo ake kukayamba moyo watsopano. Uku ndiko kutembenuka mtima.

MUNTHU WOLOWELERA

Munthu ali ngati mwana wolowelera uja. M’ moyo wake wa uchimo amatchela mbuyo yake kwa Mulungu ndi kumwamba komwe ndi kwawo. Sitepe ili yonse yomwe amatenga imamchotsa pamaso pa Mulungu kumuyandikitsa ku imfa ku imfa yauzimu yosiyantsidwa kwamuyaya ndi Mulungu. Pakufunika atapanga chiganizo chachikulu. Akuyenera “kubwelera kwa iye yekha” ndi kuzindikira za vuto lake lauzimu. Akuyenera kupanga chiganizo chomwe chimutengere kukusintha njira yake muuzimu.

KULUNGAMITSIDWA NDI CHIPULUMUTSO

Pali mau awiri m’Baibulo omwe ali pa ubale ndi mau oti kulapa. Mauwa ndi “kulungamitsidwa” ndi “chipulumutso.” Mulungu ndiye woweruza wa mtundu wonse wa anthu. Ukamakhala mu uchimo umakhala woweruzidwa pamaso pake.

Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. Koma ciweruziro ndi ici, kuti kuunika kunadza ku dziko lapansi, ndipo anthu anakonda mdima koposa kuunika; pakuti nchito zao zinali zoipa. (Yohane 3:18-19)

Ukalapa machimo ndi kupanga chisankho chochoka ku njira zako za uchimo umakhala pa ubale wabwino ndi Mulungu. Ubale wabwino umenewu kapena kuima bwino pamaso pa Mulungu uku kumatchedwa “kulungamitsidwa”:

Kusakaza ndi kusauka kuli m’njira zao; Ndipo njira ya mtendere sanaidziwa; Kumuopa Mulungu kulibe pamaso pao.

Munthu ukalungamitsidwa mwa kulapa ndi kutembenuka mtima, “umapulumsidwa” ku moyo wa uchimo komanso ku chilango cha uchimo. Izi ndi zomwe “kupulumutsidwa” kumatanthauza komanso zomwe Baibulo limatanthauza likagwiritsa ntchito mau oti “kupulumutsidwa.” (Aroma 3:16-18)

NKHONDO YAUZIMU NDI MAONEDWE A ZINTHU MOLINGANA NDI BAIBULO

Phunziro la nkondo yauzimu likuyenera kusanthulidwa molingaliranso cholinga chonse cha Mulungu populumutsa munthu wochimwa. Santhulani bwino za fanizo la Wofesa ndi Nansongole ndi Tirigu mu Mateyu 13. Mafanizo onsewa amakamba za kukula kwa Ufumu wa Mulungu komwe kumachitika kudzera nkubvala Mau a Mulungu. Mafanizo onsewa akutionetseranso nkondo ya pakati pa maufumu koma molimbana kwambiri ndi dongosolo la Mulungu lowombola munthu.

Kuphunzira za nkondo yauzimu kumakukonzekeretsani kulowa mu nkulimbanaku kumenyera nkondo miyoyo ya azimayi, azibambo, anyamata ndi atsikana. Ichi nchifukwa chake Yesu anawapatsa ophunzira ake ulamuliro pa mphamvu ya Satana asanatumizidwe kokalalikira Uthenga Wabwino (Mateyu 28:18-20). Satana ndi khamu la ziwanda zake alimbana nanu kowopsa pamene mukufunafuna kupindula miyoyo ya anthu ndi kuwabweretsa pansu pa ulamuliro wa Mulungu. Kugwiritsa ntchito ndondomeko za m’Baibulo za nkondo yauzimu kumathandizira polimbana ndi maulamuliro ndi mphamvu zomwe zimalamulira miyoyo, magulu komanso madera a dziko lapansi.

KULOWETSEDWA MU GULU LA NKHONDO LA MULUNGU

Kulapa ndi kutembenuka mtima kumabweretsa kulungamitsidwa ndi chipulumutso. Ili ndilo dongosolo la Mulungu lolowera m’gulu la nkondo la Mulungu. Ngati simunalowebe mu gulu la nkondo la Mulungu, chigawo cha “Machita-chita a luso” cha phunziro lino likupatsani mwayi wakuti mulowe. Ngati ndinu kale msilikali wa Mulungu, chigawo chimenechi chikuthandizani pamene kuthandiza ena omwe akulowa kumene.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera la mu Mfundo za Nkhondo

2. Masulirani mau oti “kulapa.”

3. Fotokozerani kufunika kwa kulapa

4. Perekani tanthauzo la mau oti “kutembenuka mtima.”

5. Fotokozerani kufunika kwa kutembenuka mtima.

6. Perekani tanthauzo la “kulungamitsidwa.”

7. Fotokozerani zomwe zimanthauza akati “kupulumutsidwa.”

8. Gwiritsani ntchito fanizo la mwana wolowelera kuti mufotokozere za kulapa ndi kutembenuka mtima.

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukhu lino)

MACHITA-CHITA A LUSO

1. Kodi munalapa ndi kutembenuka mtima? Ngati ayi, mukuyenera muime kaye pompano ndipo muchite zinthu izi:
 - Lapani machimo anu.
 - Mpempheni Yesu kuti akukhululukireni
 - Mulandireni Iye ngati Mbuye ndi Mpulumutsi wa moyo wanu.
 - Tembenukani ku moyo wanu wauchimo (tembenukani mtima).
2. Monga wokhulupilira, mukachimwa, muyeneranso kulapa. Werengani zitsanzo za m'Banibulo zili m'musizi:

ANTHU A KU AKORINTO:

Anthu a mu mzinda wotchedwa Korinto amayenera kulapa:

Tsopano ndikondwera, sikuti mwangomvedwa cisoni, koma kuti mwamvetsedwa cisoni ku kutembenuka mtima; pakuti munamvetsedwa cisoni ca kwa Mulungu, kuti tisakusowetseni m'kanthu kali konse. (2 Akorinto 7:9)

Pakuti ndiopa, kuti kaya, pakudza ine, sindidzakupezani inu otere onga ndifuna, ndipo ine ndidzapezedwa ndi inu wotere wonga simufuna; kuti kaya pangakhale cotetana, kaduka, mikwiyo, zilekanitso, maugogodi ukazitape, zodzikuza, mapokoso; kuti pakudzanso ine, Mulungu wanga angandicepse pa inu, ndipo ndingalirire ambiri a iwo amene adacimwa kale, osalapa pa codetsa, ndi cigololo, ndi kukhumba zonyansa zimene anacita. (2 Akorinto 12:20-21)

ANTHU A KU AEFESO

Akhristu a ku Aefeso anauzidwa kuti alape:

Cibvumbulutso 2:5 Poto kumbukila kumene wagwerako, nulape, nucite nchito zoyamba; koma ngari sutero, ndidzadza kwa iwe, ndipo ndidzatunsa coikapo nyali cako, kucicotsa pamalo pace, ngati sulapa.

AKHRISTU A KU PERGAMO

Mulungu anauza Akhristu a Pergamo:

Cifukwa cace lapa; ukapanda kutero ndidza kwa iwe posacedwa, ndipo ndidzacita nao nkondo ndi lupanga la m'kamwa mwanga. (Cibvumbulutso 2:16)

AKHRISTU A KU SARDI

Cifukwa cace kumbukila umo unalandira nunamvamo; nusunge nulape. Ukapanda kudikira tsono, ndidzafika ngati mbala, ndipo sudzazindikira nthawi yace ndidzadza pa iwe. (Cibvumbulutso 3:3)

AKHRISTU A KU LAODIKAYA

Onse amene ndiwakonda, ndiwadzudzula ndi kuwalanga; potero cita cangu, nutembenuke mtima. (Cibvumbulutso 3:19)

KOMA NANGA INU...

Kodi pali tchimo limene simunavomereze m'moyo wanu? Paliponse pomwe pali tchimo pakuyenera kukhala kuvomereza:

Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi. Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kucitotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:8-9)

3. Chifukwa chakuti kulapa kumafunika polandira chipulumutso, Mulungu anapanga dongosolo lakuti uthenga wa kulapa ukafikire wina aliyense. Uthenga woitanira anthu kukulapa unayamba kumveka m'Chipangano Chatsopano kudzera mu utumiki wa Yohane M'batizi:

Mau a wopfuula m'cipululu, Konzani khwalala la Ambuye, Lungamitsani njira zace; Yohane anadza nabatiza m'cipululu, nalalikira ubatizo wa kutembenuka mtima wakuloza ku cikhululukiro ca macimo. (Marko 1:3-4)

Uthenga woyamba wa Yesu unali wa Kulapa:

Ndipo ataperekedwa Yohane, Yesu anadza ku Galileya, nalalikira uthenga wabwino wa Mulungu, nanena, Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupirirani uthenga wabwino. (Marko 1:14-15)

Kulapa kunalalikidwa ndi mpingo woyamba.

Ndipo anaturuka nalalikira kuti anthu atembenuke mitima. (Marko 6:12)

Ndi kucitira umboni Ayuda ndi Ahelene wa kutembenuza mtima kulinga kwa Mulungu, ndi cikhulupiriro colinga kwa Ambuye wathu Yesu Kristu. (Macitidwe 20:21)

Lero lino, wokhulupilira wina aliyense ali ndi udindo wolalikira uthenga wa kulapa pa dziko lonse lapansi. Yesu anapereka malamulo omaliza kwa ophunzira ake kuti:

ndi kuti kulalikidwe m'dzina lace kulapa ndi 9 kukhululukidwa kwa macimo kwa 10 mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. (Luka 24:47)

Pamene mulalikira uthenga wa kulapa, mumakhala mukuitanira ena kuti alowe m'gulu la asilikari a nkondo a Mulungu. Kodi mungadzipereke nokha kuyamba kulowetsa ena m'gulu la nkondo lauzimu lalikuruli?

4. Ngati muli ndi udindo wogawa uthenga wa kulapa ndi kuitanira ena kuti alowe m'gulu la asilikari la Mulungu, mukuyenera kuzindikira zomwe zimakopa anthu kuti alape. Anthu amalapa chifukwa cha:

UBWINO WA MULUNGU

Madalitso omwe Mulungu amapereka kwa anthu osalapa, musaganize kuti ndiye kuti Mulungu akuvomereza moyo wachikunja wa anthu osalapawo. Ubwino wa Mulungu ndi njira imodzi yomwe Ambuye amagwiritsa ntchito poitanira anthu kuti atembenukire kwa Iye.

Kapena upeputsa kodi kulemera kwa ubwino wace, ndi cilekerero ndi cipiriro cace, wosadziwa kuti ubwino wa Mulungu ukubwezera kuti ulape? (Aroma 2:4)

KULALIKIRA

Kulalikidwa kwa Mau a Mulungu kumapangitsa anthu kulapa. Kulalikira kwa Yona kunabweretsa mzinda wonse wa Nineve kukulapa.

KUITANA KWA KHRISTU

Pamene Mau a Mulungu alalikidwa, anthu amamva komanso kubvomera kuitana kwa Khristu komwe kumawatsogolera kukulapa.

Koma mukani muphunzire nciani ici: Ndifuna cifundo, si nsembe ai; pakuti sindinadza kudzaitana olungama, koma ocimwa. (Mateyu 9:13)

MULUNGU, ATATE

Yesu anati palibe munthu angadze kwa Iye ngati Atate samkokera kwa Iye. Mulungu amakokera anthu kukulapa:

Kulibe mmodzi akhoza kudza kwa Ine koma ngati Atate wondituma Ine amkoka iye; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomariza. (Yohane 6:44)

KUDZUDZULA

Kudzudzula kumapangatsa anthu kulapa. Kudzudzula ndiko kukonza kuchokera m'Mau a Mulungu:

Kadzicenjerani nokha; akacimwa mbale wako umdzudzule; akalapa, umkhululukire. (Luka 17:3)

CHISONI CHA UMULUNGU:

Monga mwaphunzira kale, kulapa kumatha kuchitika pamodzi ndi zomvaimva mu mtima. Komabe kungotengeka kokha si kulapa kweni kweni, koma kudzipereka ndi mtima wonse pamaso pa Mulungu.

MAPHUNZIRO OYAMBILIRA

KUKONZEKERA KU NKHONDO

M'dziko la kuthupi palibe msilikali yemwe amatumizidwa ku nkondo analandire maphunziro oyambalilira. Maphunzirowa amamukonzekeretsa kulowa m'dera lomwe kukuchitika nkondo.

CHAPUTALA 3

WAMKULU WA NKHONDO: AMBUYE WA MAKAMU

ZOLINGA

Pomaliza pa phunziro ili mukuyenera kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera
- Kuzindikira ntchito zauzimu za kuunika
- Kuzindikira makhalidwe a Utatu Woyera
- Kufotokoza chilengedwe cha Utatu wa Umulungu
- Kufotokozerana ntchito za Mulungu Atate mu nkondo yauzimu.
- Kufotokozerana mwachidule ntchito za Yesu Khristu mu nkondo ya uzimu
- Kufotokozerana mwachidule ntchito za Mzimu Woyera mu nkondo ya uzimu.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

**Imvani, Israyeli; Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye mmodzi
(Deuteronomo 6:4)**

MAU OYAMBA

Mu chaputala 1 mudaphunzira za nkondo yaikulu yauzimu yomwe ikumenyedwa pakati pa mphamvu za kumdima ndi mphamvu zakuunika. Phunziro ili ndi linalo lifotokoza za mphamvu zauzimu zakuunika. Izi zikuphatikizapo Mulungu Atate, Mulungu Mwana, Mzimu Woyera ndi angelo. Awa ndi mphamvu zopambana zauzimu zomwe zimathandizira okhulupilira pamene akumenya nkondo.

UTATU WOYERA WA MULUNGU

Kuli milungu yambiri yomwe imapembedzedwa pa dziko lapansi, koma kuli Mulungu m’modzi yekha wona. Mulungu m’modzi ameneyu wabvumbulutsidwa m’makhalidwe atatu osiyana: Atate, Mwana Yesu Khristu ndi Mzimu Woyera.

Mulungu Tate, Yesu Khristu ndi Mzimu Woyera afotokozeredwa m’Baibulo mwa makhalidwe awo. Tikamakamba za “makhalidwe” tikutanthauza machitachita omwe amafotokozerana Mulungu. Machitachita amenewa amadziwikanso kuti makhalidwe.

Baibulo limabvumbulutsa kuti Mulungu ndi:

M’MODZI MWA ATATU

Mulungu ali ndi makhalidwe a utatu mwa m’modzi. Izi zikutanthauza kuti ali ndi makhalidwe atatu osiyana-siyana, koma ali Mulungu m’modzi:

**Imvani, Israyeli; Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye mmodzi
(Deuteronomo 6:4)**

Anthu atatu a mu Utatu Woyera wa Mulungu amatchedwa Mulungu Atate, Yesu Khristu Mwana, ndi Mzimu Woyera. Pali mavesi angapo omwe amatsimikiza za chikhalidwe cha m'modzi mwa atatu cha Mulungu. Pamene Yesu amabatizidwa ndi Yohane M'batizi mu mtsinje wa Yordano, Mulungu analankhula ndipo Mzimu Woyera anatsika:

Mateyu 3:16-17. Yesu asanabwelere kunka kumwamba atatha utumiki wake, Iye analankhula za kubwera kwa Mzimu Woyera kuchokera kwa Mulungu:

Koma pamene wafika Nkhoswe, amene Ine ndidzamtuma kwa inu kucokera kwa Atate, ndiye Mzimu wa coonadi, amene aturuka kwa Atate, Iyeyu adzandicitira Ine umboni. (Yohane 15:26)

Mtumwi Petro analankhula za chikhalidwe cha m'modzi mwa atatu cha Mulungu:

Mukatonzedwa pa dzina la Kristu, odala inu; pakuti Mzimu wa ulemerero, ndi Mzimu wa Mulungu apuma pa inu. (1 Petro 4:14)

Mtumwi Paulo analankhula za Utatu Woyera wa Mulungu m'makalata ake.

Pakuti cilamulo ca mzimu wa moyo mwa Kristu Yesu candimasula ine ku lamulo la ucimo ndi la imfa. Pakuti cimene cilamulo sicinathe kucita, popeza cinafoka mwa thupi, Mulungu anumiza Mwana wace wa iye yekha m'cifanizo ca thupi la ucimo, ndi cifukwa ca ucimo, natsutsa ucimo m'thupi; (Aroma 8:2-3)

Cisomo ca Ambuye Yesu Kristu, ndi cikondi ca Mulungu, ndi cijanano ca Mzimu Woyera zikhale ndi inu nonse. (2 Akorinto 13:14)

kuti mwa iye ife tonse awiri tiri nao malowedwe athu kwa Atate, mwa Mzimu mmodzi. (Aefeso 2:18)

Bukhu la Machitidwe limatsimikizira za chikhalidwe cha m'modzi mwa atatu cha Mulungu.

Macitidwe 2:33 Potero, popeza anakwezedwa ndi dzanja Lamanja la Mulungu, nalandira kwa Atate lonjezano la Mzimu Woyera, anatsanulira ici, cimene inu mupenya nimumva.


WAMUYAYA

Utatu wa Mulungu ndi wamuyaya ulibe chiyambi kapena chimaliziro.

Ambuye, Inu munatikhalira mokhalamo M'mibadwo mibadwo. Asanabadwe mapiri, Kapena musanalenge dziko lapansi, ndi lokhalamo anthu, Inde, kuyambira nthawi yosayamba kufikira nthawi yosatha, Inu ndinu Mulungu. (Masalmo 90:1-2)

Ndipo Abrahamu ananka mtengo wabwemba pa Beereseba, naitanira pamenepo dzina la Yehova, Mulungu wa nthawi zonse. (Genesis 21:33)

Umuyaya wa chikhalidwe cha Mulungu utha kuyerekezeddwa ndi bwalo. Bwalo silikhala ndi poyambira kapena pothera powoneka:



Chakhalidwe cha Umuyaya wa Mulungu

MZIMU

Mulungu ndi mzimu. Kutanthauza kuti alibe thupi kapena mwanzi, chotero, ndiwosaoneka ndi maso akuthupi a munthu.

Mulungu ndiye mzimu; ndipo omlambira iye ayenera kumlambira mumzimu ndi m'coonadi. (Yohane 4:24)

WAMKULUKULU

Mulungu ndi wamkulu-kulu ndi wa mphamvu zoposa pa dziko lonse. Werengani Aefeso 1 ndi Aroma 9.

WOPEZEKA PONSE-PONSE

Kutanthauza kuti amapezeka pali ponse:

Maso a Yehova ali ponseponse, Nayang'anira oipa ndi abwino. (Miyambi 15:3)

Ndidzapita kuti kuzembera mzimu wanu? Kapena ndidzathawira kuti kuzembera nkhope yanu? Ndikakwera kumka kumwamba, muli komweko; Kapena ndikadziyalira ku Gehena, taonani, muli komweko. (Masalmo 139:7-8)

WODZIWA ZONSE

Izi zikutanthauza kuti Mulungu amadziwa chili chonse:

Pakuti asanafike mau pa lilime langa, Taonani, Yehova, muwadziwa onse. (Masalmo 139:4)

m'mene monse mtima wathu utitsutsa; cifukwa Mulungu ali wamkuru woposa mitima yathu, nazindikira zonse. (1 Yohane 3:20)

Ndipo palibe colengedwa cosaonekera pamaso pace, koma zonse zikhala za pambalambanda ndi zobvundukuka pamaso pace pa iye amene ticita naye. (Ahebri 4:13)

WAMPHAMVU ZONSE

Kutanthauza kuti Mulungu angathe kuchita chili chonse:

Pamene Abram u anali wa zaka makumi asanu ndi anai kudza zisanu ndi zinai, Yehova anamuonekera Abram nati kwa iye, Ine ndine Mulungu Wamphamvuyonse; yenda iwe pamaso panga, nukhale wangwiro. (Genesis 17:1)

Ndipo Yesu anawayang'ana, nati kwa iwo, ici sicitheka ndi anthu, koma zinthu zonse zitheka ndi Mulungu. (Mateyu 19:26)

Ndipo ndinamva ngati mau a khamu lalikuru, ngati mkokomo wa madzi ambiri, ngati mau a mabingu olimba, nizinena, Aleluya; pakuti acita ufumu Ambuye Mulungu wathu, Wamphamvuyonse. (Cibvumbulutso 19:6)

Mulungu ananena kamodzi, ndinacimva kawiri: Kutu mphamvu ndi yace ya Mulungu: (Masalmo 62:11)

WOSASINTHA

Mulungu sasintha umunthu wake, chikhalidwe chake, zolinga zake kapena dongosolo lake:

Pakuti Ine Yehova sindisinthika, cifukwa cace inu ana a Yakobo simunathedwa. (Malaki 3:6)

Ahebri 13:8 Yesu Kristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi ku nthawi zonse.

WOYERA

Mulungu ndi wopanda tchimo, wangwiro kotheratu:

Nena ndi khamu lonse la ana a Israyeli, nuti nao, Muzikhala oyera; pakuti ine ndine Yehova Mulungu wanu, ndine woyera. (Levitiko 19:2)

WOLUNGAMA

Mulungu ndi wabwino komanso wosaona nkhope poweruza.

Ndipo Yehova anati kwa iye, Si ili dziko ndinalumbirira Abrahamu, Isake, ndi Yakobo, ndi kuti, Ndidzalipereka kwa mbeu zako. Ndinakuonetsa ili m'maso, koma sudzaolokako. (Deuteronomo 34:4)

WOKHULUPIRIKA

Amasunga malonjeza ano ake komanso ndi wodalarika.

ngati tikhala osakhulupirika, Iyeyu akhala wokhulupirika; pakuti sakhoza kudzikana yekha. (2 Timoteo 2:13)

WOKHUDZIKA NDI MAVUTO ATHU

Mulungu ndi wabwino ndipo amatifunira zabwino.

Yehova acitira cokoma onse; Ndi nsoni zokoma zace zigwera nchito zace zonse. (Masalmo 145:9)

WACHIFUNDO

Mulungu amaonetsa chifundo ku mtundu wa anthu wochimwa.

WODZALA NDI CHISOMO

Mulungu amaonetsera anthu chisomo chosawayenera:

popeza copfunda cace ndi ici cokha, ndico cobvala ca pathupi pace; azipfundira ciani pogona? Ndipo kudzakhala kuti akandipfuulira Ine, ndidzamva; pakuti Ine ndine wacisomo. (Eksodo 22:27)

Mulungu ndi wachisomo, wodzala ndi chifundo; woleza pakupsa mtima, ndi wa chisomo chachikulu.

Yehova ndiye wacisomo, ndi wacifundo; Osakwiya msanga, ndi wa cifundo cacikuru. (Masalmo 145:8)

WOKONDA

Mulungu ndi chikondi:

iyе wosakonda sazindikira Mulungu; cifukwa Mulungu ndiye cikondi. (1 Yohane 4:8)

WANZERU

Mulungu amaonetsera kudziwa kozama komanso wozindikira zinthu modabwitsa.

Miyambi 3:19 Yehova anakhazika dziko ndi nzeru; Naika zamwamba ndi luntha.

WOPANDA MALIRE

Mulungu ndi wopanda malire.

Palibe munthu kapena chilengedwe chomwe chingamuikire Iye malire kaya ndi a mlengalenga:

Kodi Mulungu adzakhala ndithu pa dziko lapansi? Taonani, thambo ndi m'Mwambamwamba zicepa kukulandirani, koposa kotani nanga nyumba iyi ndaimangayi. (1 Mafumu 8:27)

Kapena a nthawi:

Koma pamene Farao, anaona kuti panali kupuma, anaumitsa mtima wace, osamvera iwo; monga adalankhula Yehova. (Eksodo 8:15)

MULUNGU ATATE

Mulungu Atate ndiye wamkulu wa nkondo yauzimu yakuunika yolimbana ndi mphamvu zakumdima. Iyi ndi ntchito yake yapadera-dera mu nkondo yauzimu.

KODI MULUNGU ALI KUTI?

Mwaphunzira kale kuti Mulungu ndi waponse-ponse kutanthauza kuti amapezeka pena paliponse pa dziko lapansi. Mpando wa Chifumu uli ku otchedwa kumwamba koma amapezekansoponse-ponse.

Atero Yehova, Kumwamba ndi mpando wanga wacifumu, ndi dziko lapansi ndi coikapo mapazi anga; mudzandimangira Ine nyumba yotani? ndi malo ondiyenera kupumamo ali kuti? (Yesaya 66:1)

MAINA A MULUNGU

Baibulo limatipatsa maina ena a Mulungu omwe amabvumbulutsa utumiki wake pa inu m'kulimbana kwauzimu kwakukuru komwe kulipo. Ena mwa mainawo ndi awa:

- 1. YEHOVA:** kutanthauza kuti Ambuye. Baibulo limaphatikiza mau awa ndi maina ena a Mulungu:
 - Yehova-Rapha “Ambuye wochiritsa” Eksodo 15:26
 - Yehova-Nissi “Ambuye wokwezeka” Eksodo 17:8-15
 - Yehova-Shalom “Ambuye mtendere wathu” Oweruza 6:24
 - Yehova Ra’ah: “Ambuye m’busa wanga” Masalimo 23:1
 - Yehova-Tsidkenu: “Ambuye chilungamo chathu” Yeremiah 23:6
 - Yehova-Jireh: “Ambuye wapatsa” Genesesi 22:14
 - Yehovah-Shammah: “Ambuye alipo” Ezekiel 48:35
- 2. ELOHIM:** Kutanthauza Mulungu ndipo amagwiritsidwa ntchito paliponse pamene paonekera mphamvu yolenga ya Mulungu.
- 3. ATATE:** Machitidwe 17:28; Yohane 1:12-13
- 4. ADONAI:** Kutanthauza Ambuye. Eksodo 23:17; Yesaya 10:16, 33.
- 5. EL:** Mau awa amagwiritsidwa ntchito pamodzi ndi mau ena a Mulungu.
 - El Shaddai: “Mulungu wokwanira pa zosowa za anthu ake” Eksodo 6:3
 - Elolam: “Mulungu wosatha” Genesesi 21:33
 - El Elyon: “Mulungu wamwambamwamba wokwezedwa pamwamba pa milungu ina” Genesesi 14:18-22

6. **YAHWEH:** Mu Chihebri mau oti “Yahweh” amanthauza Mulungu. Mau awa amaphatikizidwa ndi mau ena kuti abvumbulutse zambiri za chikhalidwe cha Mulungu.

Mulungu amatchedwa:

- Yahweh Jireh: “Ambuye wopatsa” Gen. 22:14
- Yahweh Nissi “Ambuye wokwezeka” Eks. 17:15
- Yahwe Shalom “Ambuye wa mtendere” Ower. 6:24
- Yahweh Sabbaot “Ambuye wa Makamu” 1 Sam 1:3
- Yahweh Maccaddeshcem “Ambuye Wokuyeretsa” Ek 31:13
- Yahweh Tsidkeni: “Ambuye Chilungamo chathu” Yer. 23:6
- Yahweh Shammah: “Ambuye alipo” Ezek. 48:35
- Yahweh Elohim Israel “Ambuye Mulungu wa Israel” Ower. 5:3
- Quadosh Israel: “Woyera wa Israel” Yesaya 1:4

7. **AMBUYE WAMAKAMU:** M’Baibulo anthu amatchula Mulungu maina osiyana-siyana pomupempha kuti awayendere mu nyengo zawo zosiyana-siyana. Mwa chitsanzo, dzina lakuti Yehova-Rapham (Mulungu wochiritsa) limagwiritsidwa ntchito pamene apempha machiritso.

Dzina lotchulira Mulungu mwapadera mu nkondo yauzimu ndi “Yahweh Sabbaot” (Mulungu wa Makamu). Mukaitanira pa dzinali pa nkondo yauzimu, nkondoyo imasanduka ya Mulungu ndipo makamuna onse a kumwamba amatsika kukuthandizani.

MULUNGU MWANA, YESU KHRISTU

Mulungu Mwana, Yesu Khristu, amaphatikiza chikhalidwe cha Umulungu ndi cha umunthu mu mgwirizano umodzi. Mulungu Tate anatuma Yesu Khristu ku dziko lapansi monga munthu koma adakali mu Umulungu wake. Yesu anatumizidwa ndi Mulungu kubwera ku dziko lapansi kuti munthu akakhululukidwe ku uchimo.

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwa ndi iye. (Yohane 3:16-17)

Nkhani ya Yesu inalembedwa m’ mabuku a Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane m’ Baibulo. Mabuku amenewa amafotozoza mwatsatane-tsatane za kubadwa, moyo, imfa, kuuka, ziphunzitsa komanso utumuki wa Yesu Khristu.

Ngati mbali imodzi ya dongosolo la Mulungu, Yesu anabwera ku dziko lapansi monga munthu, natumikira kwa anthu, nafera machimo a anthu, naukitsidwa kwa akufa, komanso analamulira ophunzira ake kulalikira Uthenga Wabwino pa dziko lonse lapansi.

YESU ALI KUTI?

Yesu atangouka kwa akufa anaonekera kwa anthu ambiri, anatuma ophunzira ake, kenako anabwerera kunka kumwamba. Komano kumbukirani kuti ngakhale ali kumwamba, Iye amapezeka pali ponse. Kupezeka kwake kuli ponse-ponse.

NTCHITO ZAPADERA-DERA

Ntchito zapadera-dera za Yesu zokhudzana ndi nkondo yauzimu ndi izi:

1. Kuombola munthu ku uchimo: munapulumutsidwa ku ukapolo wa tchimo kudzera mu imfa ya Yesu Khristu.
ndi kuwalonjezera iwo ufulu, pokhala iwo okha ali aka polo a cibvundi; pakuti iye amene munthu agonjedwa naye, ameneyonso adzakhala kapolo wace. (2 Petro 2:19)

Cifukwa cace, abale, ife tiri amangawa si ace a thupi ai, kukhala ndi moyo monga mwa thupi; (Aroma 8:12)

Kristu anatisandutsa mfulu, kuti tikhale mfulu; cifukwa cace cirimikani, musakodwenso ndi gori la ukapolo. (Agalatiya 5:1)

2. Ulamuliro pa mphamvu zakumdima: muphunzira bwino lomwe za izi kutsogoloku. Imfa ya Yesu sinangopulumutsa munthu ku uchimo, inabweretsanso chigonjetso pa mphamvu za kumdima. Chifukwa cha ichi muli ndi mphamvu pa mdani.
Ndipo iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuciritsa nthenda. (Luka 9:1)

3. Kuononga ntchito za Satana:
iyе wocita cimo ali wocokera mwa mdierekezi, cifukwa mdierekezi amacimwa kuyambira paciyambi. Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge nchito za mdierekezi, (1 Yohane 3:8)

4. Kupempherera okhulupilira: Yesu ali ku dzanja lamanja la Mpando wa Chifumu wa Mulungu Atate kumwamba kupempherera okhulupilira omwe akumenya nkondo yauzimu. Kutanthauza kuti akulankhula kwa Mulungu Atate m'malo mwanu:
Aroma 8:34 ndani adzawatsutsa? Kristu Yesu ndiye amene adafera, inde makamaka, ndiye amene adauka kwa akufa, amene akhalanso pa dzanja lamanja la Mulungu, amenenso atipempherera ife.

MAINA A YESU

Dzina lakuti “Yesu” limatanthauza “Mpulumutsi kapena Muomboli” (Mateyu 1:21). Dzina lakuti “Khristu” limatanthauza “Wodzodzedwa” (Yohane 4:25-26). Maina ena owonjezera a Yesu opezeka m’Baibulo ndi awa:

Nkhoswe	1 Yohane 2:1
Wamphamvu zonse	Chibvumbulutso 1:8
Alefa ndi Omega	Chibvumbulutso 21:6
Amen	Chibvumbulutso 3:14
Nkhalamba ya Kale Lomwe	Daniel 7:9
Woyamba ndi Wotsiriza wa chikhulupiliro chathu	Ahebri 12:2
woyambitsa wa chipulumutso chosatha	Ahebri 5:9
Wobadwa wa Mulungu	1 Yohane 5:18
Wokondedwa	Aefeso 1:6
Nthambi	Zakariya 3:8
Mkate wa Moyo	Yohane 6:48
Nthanda	Chibvumbulutso 22:16
Wotsogolera gulu la nkondo la Mulungu	Yoswa 5:15
Mwana wa Mpalamatabwa	Mateyu 13:55
Mwala wa Pangodya	1 Petro 2:6
Wamkulu mwa Mazana Khumi	Nyimbo ya Solomoni 5:10
Khristu	Yohane 1:41
Phungu	Yesaya 9:6
Mpulumutsi	Aroma 11:26
Khomo	Yohane 10:9
Wosankhidwa	Yesaya 42:1
Emmanuel	Mateyu 1:23
Moyo Wosatha	1 Yohane 5:20
Wokhulupirika ndi Woona	Chibvumbulutso 19:11
Mboni Yoona	Chibvumbulutso 1:5
Wobadwa Woyamba	Ahebri 1:6
Woyamba ndi Wotsiriza	Chibvumbulutso 22:13
Ambuye wa Ulemelero	Yesaya 33:21
Mkulu wa Nsembe Wamkulu	Ahebri 4:14
Mutu wa Thupi	Akolose 1:18
Mutu wa Zonse	Ahebri 1:22
Mwala Wotsogoloera	Masalimo 118:22
Wolowa m'nyumba wa Zonse	Ahebri 1:2
Woyera wa Israel	Yesaya 41:14
Chiyembekezo cha Ulemelero	Akolose 1:27
Ine Ndine	Yohane 8:58
Chithunzi cha Mulungu Wosaoneka	Akolose 1:15
Yesu Khristu Ambuye wathu	Aroma 1:3
Mfumu ya Ulemelero	Masalimo 24:7
Mwana wa Nkhosa wa Mulungu	Yohane 1:29

Kuunika kwa Dziko Lapansi	Yohane 8:12
Duwa la Mzigwa	Nyimbo 2:1
Mkate wa Moyo	Yohane 6:51
Ambuye wa Mphamvu Zonse	Chibvumbulutso 4:8
Ambuye wa Onse	Machitidwe 10:36
Ambuye Chilungamo Chathu	Yeremiya 23:6
Chikondi	1 Yohane 4:8
Munthu wa Zisoni	Yesaya 53:3
Mbuye	Mateyu 23:10
Mesiya	Daniel 9:25
Woyera Wamkulu	Daniel 9:24
Mnazara	Mateyu 2:23
Mulungu wa Nzeru Yekhayo	1 Timoteo 1:17
Pasaka Wathu	1 Akorinto 5:7
Sing'anga	Luka 4:23
Mfumu ya Mtendere	Yesaya 9:6
Wophedwa m'malo mwathu	Aroma 3:25
Muomboli	Yesaya 59:20
Kuuka	Yohane 11:25
Kapolo Wolungama	Yesaya 53:11
Tanthe	1 Akorinto 10:4
Muzu wa Yese	Yesaya 11:10
Duwa la Sharon	Nyimbo 2:1
Mpulumutsi wa Dziko lapansi	1 Yohane 4:14
Mbeu ya Davide	Yohane 7:42
Mbeu ya Mkazi	Genesesi 3:15
M'busa	Yohane 10:11
Mwana wa Mulungu	Aroma 1:4
Mwana wa Munthu	Machitidwe 7:56
Mwana wa Mariya	Marko 6:3
Mwala	Mateyu 21:42
Dzulo la Chilungamo	Malaki 4:2
Maziko Eni-Eni	Yesaya 28:16
Mphunzitsi	Yohane 3:2
Choodani	Yohane 14:6
Mphatso Yosaneneka	1 Akorinto 9:15
Mpesa	Yohane 15:1
Njira	Yohane 14:6
Wodabwitsa	Yesaya 9:6

Mau
Mau a Mulungu

Yohane 1:14
Chibvumbulutso 19:13

MULUNGU MZIMU WOYERA

Mzimu Woyera ndi gawo limodzi la chikhalidwe cha m' modzi mwa atatu cha Umulungu, koma Mzimu Woyera ali ndi chikhalidwe chake chake. Phunziro la Mzimu Woyera ndi lalikulu koposa kotero kuti ndi phunziro palokha lotchedwa “Utumiki wa Mzimu Woyera” lomwe limaperekedwa ndi Harvestime International Institute. Ndipo mukulimbikitsidwa kuti mupange nawo phunziro limeneli kuti mudziwe zambiri za Mzimu Woyera.

CHIKHALIDWE CHA MZIMU WOYERA

Baibulo limabvumbulutsa kuti Mzimu Woyera:

Ali ndi maganizo:

**iyе amene sanatimana Mwana wace wa iye yekha, koma anampereka cifukwa ca ife tonse, adzalekeranji kutipatsanso ife zinthu zonse kwaulere pamodzi ndi iye?
(Aroma 8:32)**

Amafufuza maganizo a munthu

Koma kwa ife Mulungu anati onetsera izi mwa Mzimu; pakuti Mzimu asanthula zonse, zakuya za Mulungu zomwe. (1 Akorinto 2:10)

Ali ndi chifuniro

Koma zonse izi acita Mzimu mmodzi yemweyo, nagawira yense payekha monga afuna. (1 Akorinto 12:11)

Chifuniro cha Mzimu Woyera chimatsogolera okhulupilira powakaniza kuchita zinthu zina:

Ndipo anapita pa dziko la Frugiya ndi Galatiya, atawaletsa Mzimu Woyera kuti asalalikire mau m'Asiya; pamene anafika kundunji kwa Musiya, anayesa kunka ku Bituniya; ndipo Mzimu wa Yesu sanawaloleza; (Macitidwe 16:6-7)

Chifuniro cha Mzimu Woyera chimatsogolera okhulupirira powavomereza kuchita zinthu zina:

) Pamene anaona masomphenyawo, pomwepo tinayesa kuturukirakunka ku Makedoniya, poganizira kuti Mulungu anaitanira ife kulalikira Uthenga Wabwino kwa iwo. (Macitidwe 16:10)

Amalankhula:

**Ndipo Mzimu anati kwa Filipo, Yandikira, nudziphatike ku gareta uyu.
(Macitidwe 8:29)**

Amakonda

Ndipo ndikudandaulirani, abale, ndi Ambuye wathu Yesu Kristu, ndi cikondi ca Mzimu, kuti mudzalimbike pamodzi ndi ine m'mapemphero anu kwa Mulungu cifukwa ca ine; (Aroma 15:30)

Amapembedzera

Mzimu Woyera amapemphera kwa Mulungu m'malo mwa okhulupirira:

Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwiniatipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka; (Aroma 8:26)

Kuchokera mu m'ndandanda uwu wa makhalidwe a Mzimu Woyera mutha kuona kufunika kwa ntchito za Mzimu Woyera mu nkondo yauzimu. Iye amatsogolera nkondo yauzimu. Amabvumbulutsa zinthu zauzimu zomwe sizingadziwike mu umunthu. Mzimu Woyera amalankhula chifuniro ndi Mau a Mulungu kwa inu. Amapembedzeranso pamaso pa Mulungu m'malo mwanu pamene mukumenya nkondo yauzimu.

UBATIZO WA MZIMU WOYERA

Pali chinthu china chomwe chimachitika mu uzimu chotchedwa ubatizo wa Mzimu Woyera womwe umakhala ndi chizindikiro cha kulankhula malilime (Machitidwe 2) ndipo ndi umboni wa mphamvu yomwe imapangitsa kuti munthu atumikire moyenera za Uthenga Wabwino

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

Kuti mumenye nkondo yauzimu moyenera, nkofunika kuti mulandire ubatize wa Mzimu Woyera. Ili ndi gwero la mphamvu zomenyera nkondo yauzimu. Zambiri za ubatizowu zakambidwa mu phunziro lotchedwa “Utumiki wa Mzimu Woyera.”

MPHATSO ZA MZIMU WOYERA

Mzimu Woyera amapereka mphatso zapaderadera zauzimu kwa okhulupirira. Mphatsozi zafotokozeredwa bwino mu phunziro lomwe likukamba za Mzimu Woyera. Mavesi omwe amafotokoza za Mzimu Woyera ndi:

- Aroma 12:1-8
- 1 Akorinto 12:1-31
- Aefeso 4:1-16
- 1 Petro 4:7-11

Mphatso za Mzimu Woyera ndi zofunika kwambiri kuti okhulupirira azigwiritse ntchito polimbana ndi mphamvu za kumdima. Zina mwa mphatsozi ndi izi:

Mphatso zapadera zopatsa mphamvu anthu a Mulungu

Atumwi, Aneneri, Alaliki, Abusa, Aphunzitsi

Mphatso zolankhula kutambasula choonadi

Uneneri, kuphunzitsa, kudandaulira, mau a nzeru, mau a chidziwitso.

Mphatso zotumikira kuti ntchito ya Mulungu iyende bwino:

Kutumikira, kuthandiza, utsogoleri, kuweruza, kugawira, kuchita chifundo, kuzindikira mizimu, chikhulupiliro, kuchereza alendo.

Mphatso za zizindikiro kukhazikitsa ulamuliro wa Mulungu:

Malilime, kumasulira, zozizwitsa, machiritso.

CHIPATSO CHA MZIMU

Mzimu Woyera amaberekanso chipatso cha mzimu m'moyo wa okhulupilira. “Chipatso cha Mzimu” ndi chikhalidwe cha Mzimu Woyera chobvumbulutsidwa kudzera m'moyo wa okhulupirira, makhalidwe auzimu omwe akuyenera kuonekera m'moyo wa Akhristu onse.

Mphatso za Mzimu Woyera zimaonetsera mphamvu za utumuki. Chipatso cha Mzimu Woyera chimaonetsera chikhalidwe cha Umulungu m'moyo wa okhulupirira. Ngati mulibe chikhalidwe cha Khristu mwa inu, muvulazidwa koposa ndi mphamvu za kumdima. Chipatso cha mzimu ndi umboni wa kukula muuzimu. Monga m'mene zipatso za mitengo zikhallira, chipatso cha mzimu chimabwera pamene munthu akukulabe muuzimu.

Pali mitundu iwiri ya chipatso chauzimu. Chipatso chauzimu cha kubala:

Inu simunandisankha Ine, koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala cipatso, ndi kuti cipatso canu cikhale; kuti cimene ciri conse mukapempha Atate m'dzina langa akakupatseni inu. (Yohane 15:16)

Palinso chipatso chamkati chopanga makhalidwe a Khristu. Makhalidwe awa amasiyana kwatunthu ndi chikhalidwe cha thupi la munthu:

Ndipo nchito za thupi zionekera, ndizo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; zimene ndikucenjezani nazo, monga ndacita, kuti iwo akucitacita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu. Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupirtro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. (Agalatiya 5:19-23)

Ngakhale mphamvu yathupi inagonjetsedwa pa mtanda, chigonjetsochi chimapezeka kwa okhulupirira molingana ndi mlingo wa chikhulupiriro chake pa ntchito yomwe Khristu anagwira ndi kumaliza pa mtanda. Chotero, kuti muchite bwino pa kukaniza mphamvu zauchimo za thupi, nkofunika “muvale” chipatso cha Mzimu Woyera.

MZIMU WOYERA ALI KUTI

Yesu analonjeza omutsatira ake akabwerera kunka kumwamba, adzatumiza Mzimu Woyera padziko kuti akawatonthoze:

Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi yonse, ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona iye, kapena kumzindikira iye. Inu mumzindikira iye; cifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu. (Yohane 14:16-17)

Imodzi mwa ntchito za Mzimu Woyera ndi kulozera anthu kwa Khristu Yesu:

Koma pamene wafika Nkhoswe, amene Ine ndidzamtuma kwa inu kucokera kwa Atate, ndiye Mzimu wa coonadi, amene aturuka kwa Atate, Iyeyu adzandicitira Ine umboni. (Yohane 15:26)

Mulungu Mzimu Woyera, ali pa dziko lapansi lero lino koma mwauzimu ndi mosaoneka ndi maso a anthu. Iye amatumikira mu njira zosiyana-siyana pano pa dziko lapansi. Ndipo izi zalembedwa mwatsatane-tsatane mu phunziro la “Utumiki wa Mzimu Woyera” la maphunziro a Harvestime International Institute.

MZIMU WOYERA NDI WA TCHERU

Mzimu Woyera ali ndi chikhalidwe chokhala tcheru. Izi zikutanthauza kuti amakhuzika ndi zochita za anthu. Chifukwa cha ichi Baibulo limatiphunzitsa kuti tisamnamize Mzimu Woyera (Machitidwe 7:51), tisazime Mzimu (1 Atesalonika 5:19), tisamvetse chisoni Mzimu (Masalimo 78:40; Aefeso 4:30), tisamchite chipongwe Mzimu, (Ahebri 6:4-6), tisanyoze Mzimu (Mateyu 12:31-32), tisamkwiyitse Mzimu (Yesaya 63:10). Zinthu izi zakambidwanso bwino mu phunziro la “Utumiki wa Mzimu Woyera.”

Nkofunika kuti musampalamule Mzimu Woyera pakuti amakhala tcheru pa zomwe mukuchita. Mzimu Woyera akakhumudwa ndi zochita zanu amachotsa kupezeka kwake pa inu. Chotero simungathe kumenya bwino nkondo yauzimu.

MITU YA MAINA A MZIMU WOYERA

Pali mitu ingapo yomwe imagwiritsidwa ntchito pofotozera Mzimu Woyera. Mutu wa dzina umafotokozerana undido kapena ntchito ya munthu. Nkofunika kudziwa ntchito za Mzimu Woyera pamene mukulowa mu nkondo yauzimu. Onani mavesi ali m'musimu omwe mungagwiritse ntchito posanthula mitu ya maina a Mzimu Woyera.

Mzimu Woyera amatchedwa:

Mzimu wa Mulungu	1 Akorinto 3:16
Mzimu wa Khristu	Aroma 8:9
Mzimu wa Muyaya	Ahebri 9:14
Mzimu wa Choonadi	Yohane 16:13
Mzimu wa Chisomo	Ahebri 10:29
Mzimu wa Moyo	Aroma 8:2
Mzimu wa Ulemelero	1 Petro 4:14
Mzimu wa Nzeru ndi Bvumbulutso	Aefeso 1:17
Wotonthoza	Yohane 14:26
Mzimu wa Lonjezano	Machitidwe 1:4-5
Mzimu wa Chiyero	Aroma 1:4
Mzimu wa Chikhulupiriro	2 Akorinto 4:13
Mzimu wa Umwana	Aroma 8:15

ZINTHU ZOIMIRA MZIMU WOYERA

Baibulo limagwiritsa ntchito zinthu zosiyana-siyana zomwe zimaira Mzimu Woyera. Izi zimakhala zizindikiro zomwe zimakhala ndi tanthauzo lapadera-dera. Onani mavesi ali m'musiwa. Onsewa akugwiritsa ntchito chinthu china chake choimira Mzimu Woyera:

Nkhunda: Yohane 1:32; Nyimbo ya Solomo 6:9

Mafuta: Luka 4:18; Machitidwe 10:38; Ahebri 1:9

Madzi: Yohane 7:37-39; Yesaya 44:3

Chitsindikizo: Aefeso 1:13; 4:30; 2 Akorinto 1:22

Mphepo: Yohane 3:8; Machitidwe 2:1-2.

Moto: Eksodo 3:2; 13:21; Levitiko 9:24; Machitidwe 2:3

Matanthauzo a zinthu izi aperekedwa mu phunziro la “Utumiki wa Mzimu Woyera.”

KUOMBA NKOTA

Mu phunziro ili mwaphunzira za chikhalidwe cha m'modzi mwa atatu cha Mulungu komanso za Mulungu Atate, Mwana Yesu Khristu ndi Mzimu Woyera. Akaphatikizana mphamvu mu nkondo yauzimu amapanga mphamvu zodabwitsa za kuunika pa dziko lapansi.

Komabe si kuzindikira kuti mphamvu za kuunika ziripo kwakokha sikokwanira. Baibulo limati:

Ukhulupirira iwe kuti Mulungu ali mmodzi; ucita bwino; ziwanda zikhulupiranso, ndipo zinthunthumira. (Yakobo 2:19)

Mphamvu zauzimu zakumdima zimadziwa kuti Mulungu alipo ndipo zimanthunthumira, koma zimakhalabe zoipa. Kungokhulupirira mwa Mulungu kokha sikokwanira. Mukuyenera kumudziwa ndi kumvomereza ngati Mbuye wa Moyo wanu. Mukuyenera kulandira nsembe ya Yesu Khristu yoperekedwa chifukwa cha machimo anu, kulapa, kupempha chikhululukiro ndi kukhala wolengedwa watsopano mwa Khristu.

Simunatsirize phunziro la mphamvu zauzimu zakuunika. Chaputala chotsatirachi chikukamba za gulu lalikulu la mphamvu la angelo ndi kufotokoza za ntchito yawo mu nkhondo yauzimu.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo

2. Lembani mphamvu zakuunika zauzimu

3. Tchulani magawo atatu a Utatu wa Mulungu

Mulungu _____

Mulungu _____

Mulungu _____

4. Lembani mwachidule ntchito za Mulungu mu nkhondo yauzimu.

5. Lembani mwachidule ntchito za Yesu Khristu mu nkhondo yauzimu.

6. Lembani mwachidule ntchito za Mzimu Woyera mu nkhondo yauzimu.

7. Kodi ndi dzina liti la Mulungu lomwe mukuyenera kugwiritsa ntchito pamene mukulowa mu nkhondo yauzimu.

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukhu lino).

MACHITA-CHITA A LUSO

Maphunziro ena okhuzana ndi moyo, utumiki, ndi ziphunzitso za Yesu ziri mu phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa “*Kukhala Moyo wa mu Ufumu*” ndi “*Luso la Kaphunzitsidwe.*”

Phunziro la Harvestime International Institute Lotchedwa “Maziko a Chikhulupiriro” limapereka tsatane-tsatane wa chiphunzitso cha chikhulupiriro cha Chikhristu. Ndipo ndilofunika kwambiri pakumvetsa bwino za mphamvu zauzimu zakuunika.

Kodi mukukumana ndi nkondo yauzimu? Pamene mukupempherera za vuto lanu, yambani kuitanira pa dzina la Ambuye wa Makamu.

Tangoganizirani za nkondo yomwe mukudutsamo tsopano lino, ndiye muwerengenso z ant hito ya Mulungu Atate, Yesu Khristu ndi Mzimu Woyera pa nkondo yauzimu. Kodi Mulungu angakuthandizeni motani mu nkondo yanu? Kodi Yesu angakuthandizeni motani? Kodi ntchito za Mzimu Woyera ndi zotani pa vuto lomwe mukukumana nalo.

CHAPUTALA 4

MPHAMVU ZA UZIMU ZA KUUNIKA: ANGELO

ZOLINGA

Mukamaliza phunziro ili mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kupereka mavesi ofotokozerana chimene angelo ali.
- Kunena chiyambi cha angelo
- Kuzindikira mitundu iwiri ya angelo
- Kuzindikira komwe amagwirira ntchito.
- Kufotokozerana mwachidule za utumiki wa angelo mu nkondo yauzimu.
- Kuzindikira makhalidwe a angelo
- Kuzindikira magulu osiyana-siyana a angelo.
- Kupereka vesi lofotokozerana dongosolo la momwe gulu la angelo amagwirira ntchito

VESI LOCHOKERA MU MFUNDO ZA NKONDO

**Adzabukitsa cikumbukilo ca ubwino wanu waukuru, Nadzayimbira cilungamo canu.
(Masalmo 145:7)**

MAU OYAMBA

Mu chaputala chapitachi mwaphunzira za Utatu Woyera wa Mulungu momwe muli Mulungu Atate, Mulungu Mwana Yesu Khristu, ndi Mulungu Mzimu Woyera. Mwaphunzira chiyambi chawo, makhalidwe awo, komanso ntchito zawo mu nkondo yauzimu.

Chaputala chino chikupitiriza pa phunziro la mphamvu zauzimu za kuunika. Chikufotokozerana chiyambi, makhalidwe, dera la ntchito, magulu, komanso dongosolo la magwiridwe a ntchito a angelo. Chikufotokozeranso utumiki wao mu nkondo yauzimu.

ANGELO NDI NDANI?

Angelo ndi mizimu yotumikira yotumidwa ndi Mulungu kukachita chifuniro chake:

Ahebri 13:14 Pakuti pano tiribe mudzi wokhalitsa, komatu tifunafuna ulinkudzawo.

Mau oti “mngelo” limatanthauza mtumiki.

CHIYAMBI CHA ANGELO

Angelo analengedwa ndi Mulungu:

Mlemekezeni, angelo ace onse; Mlemekezeni, makamu ace onse. Alemekenze dzina la Yehova; Popeza analamulira, ndipo zinalengedwa. (Masalmo 148:2,5)

pakuti mwa iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yacifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa iye ndi kwa iye.

(Akolose 1:16)

Angelo onse anali olungama ndi oyera pamene analengedwa poyamba. Anapembedza ndi kutumikira Mulungu m' modzi Woon. Kenako, angelo ena anaukira Mulungu ndi kutaya undido wawo wokhala angelo (wotumikira). Iwo anakhala mbali imodzi ya mphamvu za kumdima zotchedwa “ziwanda.”

Tsopano tili ndi magulu awiri a angelo: Angelo abwino, omwe ndiye mutu wa chaputala chino, ndi angelo oyipa (ziwanda) omwe tiwaone mu chaputala 6 cha phunziro lino.

DONGOSOLO LA MAGWIRIDWE NTCHITO A ANGELO

Mulungu waika angelo abwino mu dongosolo lapadera-dera. Baibulo silifotokoza mwatsatane-tsatane za dongosololi koma limaonetsa kuti dongosololo lilipo.(Akolose 1;16; Onaninso Aefeso 3:10).

Dongosolo la dziko losaonekali lafotokozeredwa monga mafumu, akuluakulu, aulamuliro, ndi amphamvu. Zitinapatsidwe tsatane-tsatane wa dongosolo ili. Muona patsogolopa momwe Satana watengera dongosololi poika dongosolo la mphamvu zake za kumdima.

MAGULU A ANGELO

Kuli miyanda-miyanda ya angelo (Luka 2:13-15) omwe aikidwa m' magulu-magulu molingana ndi ntchito zomwe amagwira. Magulu eni eni ndi awa:

ATUMIKI

Gulu ili ndiye ndi lomwe litha kukhala ndi angelo ochuluka mwa magulu onse. Awa ndi angelo omwe ali mgulu la angelo osawerengeka lomwe Daniel analiona m' masomphenya (Daniel 7:10), omwe amakwaniritsa chifuniro cha Mulungu kumwamba komanso pa dziko lapansi. Ili ndi gulu lomwe limakhala pafupi ndi okhulupilira mu nkondo yauzimu. Angelowa amamasulira chifuniro cha Mulungu, kuteteza, kupereka chitsogozo, kubweretsa mayankho a mapemphero, kulengeza, kuchenjeza, kulangiza, kubweretsa chiweruzo, kulimbikitsa, kugwiriziza, kupulumutsa, kupembedzera m' malo mwa okhulupilira.

ANGELO OSANKHIDWA

Pali vesi limodzi lokha lomwe likukamba za gulu ili la angelo (1 Timoteo 5:21). Palibenso mau ena okhuza gulu limeneli omwe aperekedwa.

AKERUBI

Gulu ili latchulidwa koyamba mu Genesis 3:24. Atchulidwanso ngati gawo limodzi la Likasa la Chipangano (Eksodo 25:18-22). Ezekiel akutchulako zolengedwa izi ndi kuzifotozera monga

zokhala ndi maonekedwe anayi; nkhope ya mkango, nkhope ya ng'ombe, nkhope ya munthu ndi nkhope ya chiomba nkhangha (Ezekiel 1:3-28; 10:22). Zizindikiro za akerubi zikuonetseratu kuti ndi zolengedwa zamoyo zokhala mozungulira Mpando wa Chifumu wa Mulungu in Chibvumbulutso 4:6. Akupezeka mu gawo lapamwamba kwambiri m'magulu a angelo popeza amayang'anira Mpando wa Chifumu wa Mulungu.

ASERAPHI

Gulu ili latchulidwa mu Yesaya 6:2, 6. Malo awo ali pamwamba pa Mpando wa Chifumu wa Mulungu mosiyana ndi akerubi omwe amakhala mozungulira mpandowu. Zikuonetsa kuti ntchito yawo ndi kutsogolora gulu lonse la kumwamba nkupembedza Mulungu.

ZOLENGEDWA ZAMOYO

Gulu ili latchulidwa mu Chibvumbulutso 4:6, 8; 5:6. Dzina la angelo awa limaonetsa chidzalo cha moyo wa Umulungu ndipo utumiki wawo ndiwopembedza Mulungu basi.

ANGELO PAOKHA PAOKHA

Kuonjezera pa magulu osiyana-siyana a angelo, pali angelo ena omwe atchulidwa maina m'Baibulo.

MIKAELE

Mikaele, mngelo wamkuru, watchulidwa ndi dzina mu Daniel 10:13, 21, 12:1; Yuda 9 ndi Chibvumbulutso 12:7. Ndi mngelo yekhayo amene amatchulidwa kuti “wamkulu.” Amafotokozeredwa moonetsa kuti ndiye wolamulira angelo a nkondo mu Chibvumbulutso 12:7 ndipo watchulidwa kuti ndi mfumu ya ana a Israel mu Daniel 10:13, 21; 12:1.

GABRIEL

Tanthauzo la dzinali ndi “wamphamvu.” Watchulidwa mu Daniel 8:16; 9:21 ndi Luka 1:19, 26. Nthawi zambiri amagwiritsidwa ntchito kukatula uthenga wochokera kwa Mulungu. Ndi Gabriel yemwe anatanthauzira masomphenya kwa Daniel mu chaputala 8:16, 9-21 komanso analengeza za kubadwa kwa Yohane ndi Yesu mu Luka 1:19, 26.

MAGULU A PADERA-DERA A ANGELO

Baibulo limatchulanso magulu ena a padera a angelo omwe ndi:

Angelo a mipingo isanu ndi iwiri: Chibvumbulutso 1:20

Angelo anayi olamulira mphepo: Chibvumbulutso 1:7

Angelo asanu ndi awiri oimilira pamaso pa Mulungu: Chibvumbulutso 8:2

Angelo asanu ndi awiri omwe adzabwere ndi miliri isanu ndi iwiri yomaliza Chibvumbulutso 15:1, 7.

Akulu makumi awiri kudza mphambu zinayi (angelo)

Chibvumbulutso 4 ndi 5.

MAKHALIDWE A ANGELO

Mutha kukumbukira kuchokera mu chaputala chapitachi kuti chikhalidwe ndi umunthu kapena machita-chita a munthu. Angelo...:

- Ndi mizimu: Ahebri 1:14
- Kulibe angelo akazi kapena amuna: Luka 20:34-36
- Samafa Mateyu 22:28-30
- Nthawi zina amaoneka koma nthawi zina saoneka: Numeri 22:22-3
- Amaoneka ngati munthu: Genesis 19:1-22; 18:2,4,
- Amakondwa kapena kukwiya: Luka 15:1-10 (angelo kusangalala).
- Amakhala ndi chilakolako cha chakudya: Genesis 18:8
- Ndi a ulemelero: Luka 9:26
- Ndi a nzeru: 2 Samuel 14:20
- Ndi ofatsa: Juda 9
- Ndi amphamvu: Masalimo 103:20; 2 Petro 2:11
- Sasoweka kupuma: Chibvu. 4:8
- Amayenda mwa change chosawerengeka: Chibvu. 8:13; 9:1
- Amalankhula zilankhulo: 1 Akorinto 13:1
- Ndi osawerengeka: Luka 2:13; Ahebri 12:22; Masalimo 68:17; Marko 1:13; Chibvu. 5:19
- Samafa: Luka 20:34-36
- Sakwatira kapena kukhala ndi ana: Luka 20:34-36
- Ndi omvera: Masalimo 103:20
- Ndi oyera: Chibvu. 14:10; Marko 8:38
- Ndi aulemu: Ntchito yawo yaikulu ndi kupembedza Mulungu. Nehemiya 9:6; Afilipi 2:9-11; Ahebri 1:6

DERA LAWU LOGWIRA NTCHITO

Angelo ndi amagwira ntchito kumwamba komanso padziko. Gwero la mphamvu linaperekedwa komanso limayendetsedwa ndi Mulungu. Ali ndi mwayi wopezeka pamaso pa Mulungu kumwamba.

Yang'anirani kuti musanyoze mmodzi wa ang'ono awa; pakuti ndinena kwa inu, kuti angelo ao apenya cipenyere nkhope ya Atate wanga wa Kumwamba. (Mateyu 18:10)

Iwo amagwira ntchito pa dziko. Izi zatsimikizika malingana ndi mautumiki awo komanso kuoneka kwawo pamaso pa anthu osiyana-siyana m'Baibulo.

UTUMIKI WA ANGELO

Angelo amatumikira mu njira zambiri kumwamba ndinso panso pano. Werengani mavesi omwe ali m'musiwa. Pamene muwerenga ndime zimenezi mudzazindikira kufunika kwa angelo mu nkondo yauzimu.

Utumiki wa angelo kumwamba:

- Kupembedza: Chibvu. 4:8; 5:11-12; Yesaya 6:3; Masalimo 103:20; 148:1-2
- Kukhala wodikira kuchita chifuniro cha Mulungu: Masalimo 103:20-21
- Kutumikira omwe adafa akutumikira Khristu: Juda 9; Luka 16:22
- Kuimilira ana mwapadera: Mateyu 18:10
- Kukondwera chifukwa cha iwo amene alandira Uthenga Wabwino: Luka 15:10

Utumiki wa angelo panso pano:

- Kulamulira maiko: Daniel 10
- Kutumikira okhulupirira mnyengo ya kuyesedwa: Mateyu 4:11
- Kulimbikitsa okhulupirira: Luka 22:43
- Kutanthauzira chifuniro cha Mulungu kwa anthu: Zekariya 1:9; Daniel 7:16
- Kutsogolera okhulupirira: Machitidwe 8:26.
- Kubweretsa chiweruzo kwa anthu ndi maiko: Machitidwe 12:23; Genesis 19:3; 2 Samuel 24:16; Chibvu. 16:1
- Kubweretsa mayankho a mapemphero: Daniel 9:21-22
- Kulengeza: Luka 1:11-20; Mateyu 1:20, 21
- Kuchenjeza: Mateyu 2:13;
- Kulangiza: Mateyu 28:2-6;
- Machitidwe 10:3-6; Daniel 4:13-17
- Kulimbikitsa: Machitidwe 27:23; Genesis 28:12
- Kubvumbulutsa: Machitidwe 7:53; Agalatiya 3:19; Ahebri 2:2; Daniel 9:21-27; Chibvu. 1:1
- Kupatsa mphamvu: Mateyu 4:11; Luka 22:43
- Kusunga: Genesis 16:7; 24:7; Eksodo 23:20; Chibvu. 7:1
- Kuteteza: Masalimo 91:11
- Kumasula: Numeri 20:16; Masalimo 34:7; Yesaya 63:9; Daniel 3:28; 6:22; Genesis 48:16; Mateyu 26:53; Machitidwe 12:1-19
- Kuononga: Machitidwe 12:20-23
- Kupembedzera: Zekariya 1:12; Chibvu. 8:3, 4

Ntchito za angelo mtsogolomu:

- Kutanga nawo mbali pakubweranso kwa Yesu: 1 Atesalonika 4:16
- Kusonkhanitsa osankhika: Mateyu 24:31
- Kuchenjeza ndi kulalikira nthawi ya chisautso chachikuru: Chibvu. 14:6-9

- Kusiyanitsa ochimwa ndi olungama: Mateyu 13:39 and 49
- Kumanga Satana: Chibvu. 20

ANGELO NDI NKHONDO YAUZIMU

Angelo otumikira ali m'gulu la angelo lomwe limakhala pafupi ndi okhulupirira pa nkondo yauzimu. Amamasulira chifuniro cha Mulungu, amateteza, amapereka chitsogozo, amabweretsa mayankho a mapemphero, amalengeza, amachenjeza, amalangiza, amabweretsa chiweruzo, amalimbikitsa, amasunga, amamasula komanso kupembedzera m'malo mwa okhulupirira pomenya nkondo.

Okhulupirira ambiri sakhumba konse thandizo lomwe angelo amapereka pomenya nkondo yauzimu chifukwa chakuti sanaphunzitsidwe za ntchito ya angelo pa nkondo yauzimu. Angelo ndi “mizimu yotumikira” ndipo atha kukutumikirani komanso kutumikira m'malo mwanu. Mungathe kupempha Mulungu kuti akutumizireni angelo okhuthandizani m'nkondo. Mfumu Davide anachita ichi. Iye anapemphera....

Akhale monga mungu kumphepo, Ndipo mngelo wa Yehova awapitikitse. Njira yao ikhale ya mdima ndi yoterera, Ndipo mngelo wa Yehova awalondole.
(Masalmo 35:5-6)

Werengani zomwe Baibulo likulankhula za angelo omwe amatithandiza polimbana ndi m'dani: 2 Mafumu 19:35; 2 Mbiri 32:21; Yesaya 37:36; Chibvu. 12:7.

MACHENJEZO OFUNIKIRA

Angelo ndi zolengedwa zoyera zomwe zili ndi utumiki wofunikira m'malo mwa okhulupirira. Ali mbali imodzi ya mphamvu za kuunika momwe ulili Utatu Woyera. Mau a Mulungu amatichenjeza za kupembedza angelo:

OSAMAPEMBEDZA ANGELO:

Simukuyenera kupembedza angelo:

Munthu ali yense asakunyengeni ndi kulanda mphotho yanu ndi kudzicepetsa mwini wace, ndikugwadira kwa angelo, ndi kukhalira mu izi adazona, wodzitukumula cabe ndi zolingalira za thupi lace, wosagwiritsa mutuwo,
(Akolose 2:18)

Ndipo ine Yohane ndine wakumva ndi wakupenya izi. Ndipo pamene ndinamva ndi kupenya, ndinagwa pansu kulambira pa mapazi a mngelo wakundionetsa izo. Ndipo ananena kwa ine, Tapenya, usacite; ndine kapolo mnzako, ndi mnzao wa abale ako aneneri, ndi wa iwo akusunga mau a buku ili; lambira Mulungu.
(Cibvumbulutso 22:8-9)

KANANI ULALIKI WA ANGELO “UTHENGA WINA”

Anthu ena amanena kuti aona angelo akuwapatsa “bvumbulutso latsopano” losemphana kutali ndi Mau a Mulungu. Mipingo yambiri idayamba kudzera m’ mabvumbulutso a bodza. Baibulo limachenjeza kuti:

**Ndipo kulibe kudabwa; pakuti Satana yemwe adzionetsa ngati mngelo wa kuunika.
(2 Akorinto 11:14)**

OSAKWIYITSA ANGELO

Werengani nkhani ya Balaam mu Numeri 22, za m’ neneri yemwe anachita kusamvera pamaso pa Mulungu. Mutha kuona kuti anadzudzulidwa ndi mngelo wa Ambuye. Mukakhala osamvera pamaso pa Mulungu, angelo atha kukutchingani. Mukhala mukumenyana nkondo koma osati ya kumdimba ayi. Mukhale osamala ndi kusakwiyitsa kapena kukhumudwitsa angelo a Mulungu.

Samalira phazi lako popita ku nyumba ya Mulungu; pakuti kuyandikira kumvera kupambana kupereka nsembe za zitsiru; pakuti sizizindikira kuti zirikucimwa. Usalankhule mwanthuku mtima wako, usafulumire kunena kanthu pamaso pa Mulungu; pakuti Mulungu ali kumwamba, iwe uli pansu; cifukwa cace mau ako akhale owerengeka. Pakuti loto lafika mwakucuruka nchito; ndipo mau a citsiru mwakucuruka maneno. Utawinda ciwinda kwa Mulungu, usacedwe kucicita; pakuti sakondwera ndi zitsiru; cita comwe unaciwindaco. Kusawinda kupambana kuwinda osacita, Usalole m'kamwa mwako mucimwitse thupi lako; usanene pamaso pa mthenga kuti, Ndinaphophonya; Mulungu akwiye mau ako cifukwa ninji, naononge nchito ya manja ako? (Mlaliki 5:1-6)

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Angelo amatumikira _____ ndi _____
3. Kodi angelo anachokera kuti?

4. Lembani mwachidule za utumiki wa angelo molingana ndi nkhondo yauzimu.

5. Lembani makhalidwe a angelo omwe mungathe kuwakumbukira kuchokera mu chaputala chino.

6. Perekani vesi yomwe imafotokozera chomwe angelo ali.

7. Kodi mau awa ndi owona kapena ayi? Osapembedza angelo. Mau awa ndi

8. Kodi mau awa ndi owona kapena ayi? Ngati mngelo awonekera kwa inu nabvumbulutsa chinthu china chomwe chikusemphana ndi Mau a Mulungu mumvere popeza watumidwa kuchokera kwa Mulungu. Mau awa ndi _____
9. Gwiritsani ntchito mau ali m'musiwa powaika malo omwe akuyenera kukhala mu ndime zili m'musizi.
Atumiki.
Angelo osankhidwa
Akerubi
Aserafi
Zamoyo zinayi
_____ Pali vesi limodzi lokha lomwe limatchula zagulu ili la angelo (1 Timoteyo 5:21). Palibe china chomwe chimamveka m'Baibulo cha iwo.
_____ Gulu ili la angelo ndi lochitachita kwambiri maka pa nkhondo yauzimu komanso mwina ndiye gulu lochuluka kwambiri la angelo.
_____ Gulu ili la angelo limaoneka kuti ndiye lapamwamba kwambiri mu dongosolo la angelo; olondera mpando wa Mulungu. Amazungulira mpando wa Mulungu. Ntchito yawo yaikulu ndi yolambira Mulungu.
_____ Malo awo ali pamwamba pa mpando wa Mulungu. Amatsogolera gulu la kumwamba pa kupembedza Mulungu.
10. Pali magulu awiri a angelo: Maguluwa ndi: _____ ndi
_____ omwe amatchedwanso ziwanda.

11. Kodi ndi vesi lanji lomwe limaonetsa kuti Mulungu ali ndi dongosolo la magwiridwe ntchito a magulu a angelo.

(Mayankho a mafunso wa ali kumapeto kwa buku lino)

MACHITA-CHITA ALUSO

1. Gwiritsani ntchito ndondomeko yotsatirayi popiriza kuphuzira za angelo:

ANGELO M'CHIPANGANO CHAKALE

Anapululumutsa Hagar: Genesis 16:7-12
Analengeza za kubadwa kwa Isaki: Genesis 18:1-15
Analengeza za kuonongedwa kwa Sodom: Genesis 18:16-33
Anaononga Sodom sapulumutsa Loti: Genesis 19:1-29
Analetsa kuphedwa kwa Isaki: Genesis 22:11-2
Analondera Yakobo: Genesis 28:12; 31:11; 32:1; 48:16
Anatuma Mose: Eksodo 3:2
Anatsogolera Israel: Eksodo 14:19; 23:20-23; 32:34
Anakonza dongosolo la ukwati wa Isaki ndi Rabeka: Genesesi 24:7
Anapereka Chilamulo: Machitidwe 7:38; Agalatiya 3:19; Hebrews 2:2
Anadzudzula Balaam: Numeri 22:31-35
Anaonekera kwa Yoswa: Yoswa 5:13-15
Anadzudzula Israel chifukwa cha mafano: Oweruza 2:1-5
Anatuma Gideon: Oweruza 6:11-40
Analengeza za kubadwa kwa Samson: Oweruza 13
Analanga Israel: 2 Samuel 24:16-17
Anapululumutsa Eliya: 1 Mafumu 19:5-8
Anazungulira Elisa: 2 Mafumu 6:14-17
Anapululumutsa Daniel ku mikango yolusa: Daniel 6:22
Anagonje a Asuri ku nkondo: 2 Mafumu 19:35 ndi Yesaya 37:36
Amaima pozungulira ana a Mulungu: Masalimo 34:7; 91:11
Nthawi zambiri amatchedwa atumiki a aneneri a Mulungu.

ANGELO M'MOYO WA YESU

Analengeza za kubadwa kwa Yohane: Luka 1:11-17
Anamutchula dzina: Luka 1:13
Analengeza za kubadwa kwa Yesu kwa Mariya: Luka 1:26-37
Analengeza za kubadwa kwa Yesu kwa Yosefe: Mateyu 1:20-21
Anamutchula dzina Yesu: Matthew 1:21
Analengeza za kubadwa kwa Yesu kwa abusa: Luka 2:8-15
Anaimba: Luka 2:13-14
Anatsogolera kuthawa kupita ku Aigupto: Mateyu 2:13,20
Anatumikira Yesu nthawi ya mayesero ake: Mateyu 4:11
Anabwera kwa Yesu m'munda wa Getseman: Luka 22:43
Anachotsa mwala pa manda a Yesu: Mateyu 28:2
Analengeza za kuuka kwake kwa akufa: Mateyu 28:5-7

Anampereka Iye pamaso pa Maria Magdalene: Yohane 20:11-14
Angelo anamkwezetsa Iye kunka kumwamba: Yohane 1:51
Anali chinamtindi cha angelo: Mateyu 26:53

Angelo adzabwera naye limodzi: Mateyu 25:31; 16:27; Marko 8:38;
Luka 9:26

Angelo adzakhala okolora: Mateyu 13:39
Adzasonkhanitsa osankhidwa: Mateyu 24:31
Adzasiyanitsa olungama ndi ochimwa: Mateyu 13:41,49
Anamtengera wopempha uja kwa Abraham: Luka 16:22
Amakondwera pamene wochimwa walapa: Luka 15:10
Amaimirira ana ang'onoang'ono: Mateyu 18:10
Adzavomereza ake pamaso pa angelo: Luka 12:8
Si amuna kapena akazi komanso samafa: Luka 20:35-36
Satana ali ndi angelo oyipa: Mateyu 25:41

ANGELO M'BUKU LA MACHITIDWE A ATUMWI

Anatsegula makomo a ndende: 5:19
Anamtsogolera Filipo kwa Mdindo wa ku Aitopia: 8:26
Anatsogolera Koneliyo kuitana Petro: Chapter 10
Anamasula Petro ku ndende: 12:7-19
Anamkantha Herodi mpaka kufa: 12:23
Anaima naye Paulo m'mafunde: 27:23
Atchulidwanso mu: 6:15; 7:30,35,38,53; 11:13; 23:8-9

ANGELO M'MAKALATA:

Angelo osankhidwa: 1 Timoteyu 5:21
Angelo ngwosawerengeka: Ahebri 12:22
Angelo amatumikira opulumutsidwa: Ahebri 1:13-14
Angelo adzabwera ndi Yesu: 2 Atesalonika 1:7
Sitikuyenera kupembedza angelo: Akolose 2:18

ANGELO M'BUKU LA CHIBVUMBULUTSO

Anatsogolera nkulembedwa kwa Buku la Chibvumbulutso : 1:1-2; 22:16
Amayang'anira mipingo isanu ndi iwiri: Chapters 1-2
Anali ndi chidwi ndi buku lotsindikizidwa: 5:2
Anayimba nyimbo zolemkeza mwana wa nkhosa: 5:11-12
Anapatsidwa mphamvu zapadera pa dziko: 7:1-4
Anasindikiza osankhidwa: 7:1-4
Anagwa pansu pamaso pa Mulungu: 7:11
Anagwiritsidwa ntchito kuyankha mapemphero a okhulupirira: Anaomba malipenga asanu ndi

awiri: 8:6

Analamulira gulu la dzombe: 9:11

Anamasula a pakavalo 200, 000, 000: 9:15-16

Analengeza za kutha kwa dziko: 10:1,2,6

Anamenyana ndi chinjoka ndi amithenga ake: 12:7

Analalikira Uthenga Wabwino ku maiko: 14:6

Analankhula za kugwa kwa Babulo: 14:8; 18:2

Analengeza za tsoka la otsatira chirombo: 14:9-10

Analengeza za kholola pa dziko: 14:15-18

Anali ndi miliri isanu ndi iwiri yomaliza: 15:1

Analengeza za chiweruzo cha Babulo: 17:1,5

Anatenga nawo mbali pa kugwa kwa Babulo: 18:21

Anamuonetsa Yohane Yerusalemu Watsopano: 21:9

Anamuletsa Yohane kuti asawapembedze: 22:8-9

2. Santhulani za kuonekera kwa angelo mu Oweruza 13. Onani kuti m'ngelo abwelera kumwamba kudzera m'kupembedza kubzola "m'dziko la Satana mlengalenga" motizungulira kulola angelo kuti agwire ntchito m'malo mwathu. Onaninso nkhani ya Daniel ndipo muone kuti chotchinga cha mfumu yak u Perezi chinaphwasulidwa kudzera nkusala kudya ndi kupemphera.

3. Palibe ndime yomwe imatiuza kuti wokhulupirira angalamulire mngelo wake kuti achite zomwe akufuna, koma mungathe kumfunsa Mulungu kuti atomize angelo kugwira ntchito m'malo mwanu. Taganizani za nkhalo yomwe mukukumana nayo panopa ndipo mumfunse Mulungu kuti atumize "mizimu yotumikira" kuti igwire ntchito m'malo mwanu.

4. Werengani Masalimo 78:36, 40 ndi Mlaliki 5:6. Aisraeli anali ndi mngelo yemwe amawasamalira kufikira atamukwiyitsa m'chipululu. Ngati Mulungu angatumize wake kwa inu kuti akuthandizeni, ndiye inu ndikumukwiyitsa kudzera mu uchimo ndi kusakhulupirira, mngeloyo adzakuchokerani. Ndibwino kumvera chenjezo la pa Eksodo 23:20-22. Muthanso kuchereza mngelo inu osadziwa. Werengani Ahebri 13:2.

CHAPUTALA 5

MDANI: SATANA

ZOLINGA

Mukamaliza chaputala chino mukwanitsa kuchita izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
- Kumdziwa Satana monga mdani wanu wauzimu.
- Kufotokozero komwe kudachokera Satana.
- Kulongosola udindo wake woyamba
- Kufotokozero momwe Satana anagwera kuchoka pa malo ake oyamba.
- Kuzindikira zotsatira za tchimo la Satana.
- Kulemba mndandanda wa makhalidwe a Satana.
- Kuzindikira dera lake logwirira ntchito.
- Kuomba mkota wa ntchito za Satana.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire: (1 Petro 5:8)

MAU OYAMBA

M'machaputala a m'mbuyomu mwaphunzira za nkondo yauzimu yosaoneka yomwe ikuchitika m'dziko lauzimu. Mwaona za mphamvu za kumdima mu nkondo imeneyi ndipo izi ndi Mulungu Atate, Mwana, Mzimu Woyera ndi angelo.

Chaputala chino chikufotokozero za mdani wanu muuzimu, mphamvu yaikulu ya kumdima yotchedwa Satana. Muphunzira za chiyambi chake, udindo wake woyamba, momwe adagwera kuchoka kumwamba, ndi omwe adatsika nawo pamodzi. Muphunziranso za makhalidwe ake, dera lake logwirira ntchito ndipo muonanso njira zomwe amagwiritsa ntchito. M'machaputala awiri otsatirawa mupitiriza kuphunzira za mphamvu za kumdima pamene mukhale mukuphunzira za ziwanda, dziko ndi thupi.

Nkhondo ya kuthupi, msilikari ayenera kuzindikira mdani wake kaye asanayambe kumenya nkondo. Ayenera kudziwa zonse zokhuza mdani wakeyo: chikhalidwe chake ndi njira zake. Ichi ndi chifukwa chake asilikari ankhondo amatenga nthawi yaitali akungochita kafukufuku wa adani awo.

Izi zili chimodzimodzi ndi nkondo yauzimu. Mungathe kumenya bwino nkondo pamene mwazindikira mdani wanu, kumvetsa chikhalidwe chake komanso njira zake. Monga mwaphunzira kale, mphamvu zakumdima zomwe mukulimbana nazo si zakuthupi. Ndi makamu auzimu a choipa.

CHIYAMBI CHA SATANA

Satana analengedwa ndi Mulungu:

Zonse: zinalengedwa ndi iye; ndipo kopanda iye sikunalengedwa kanthu kali konse kolengedwa, (Yohane 1:3)

pakuti mwa iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yacifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa iye ndi kwa iye. (Akolose 1:16)

Mulungu salenga choipa. Satana anali wangwiro pamene analengedwa ndi Mulungu, koma anapatsidwa ufulu wosankha chabwino kapena choipa:

Unali wangwiro m'njira zako cilengedwere iwe, mpaka cinapezeka mwa iwe cosalungama. (Ezekieli 28:15)

UDINDO WAKALE WA SATANA

Baibulo limafotokozera za udindo wakale wa Satana mu Ezekiel 28:12-17. Musanapilire ndi phunziro lino werengani kaye ndime imeneyi. Pamene Satana analengedwa anali mngelo wa Mulungu. Anali gulu la angelo lotchedwa Akerubi, woyera, wamzeru, wokonhola, ndi wangwiro. Iye anali mtsogoleri pakati pa Akerubi ndi amatchedwa kerubi “wolondera” kapena “wophimba.” Dzina lake loyamba anali Lusifala kutanthauza kuti “wonyamula kuunika” (Yesaya 14:12). Lusifala anakongoletsedwa ndi miyala ya mtengo wapatali ya golide (Ezekiel 28:13; Eksodo 28:15). Anapatsidwa mpando pa phiri la Mulungu loyera ndipo mwina amatsogoleranso kupembedza Mulungu (Ezekiel 28:13).

Baibulo likutipatsa chithunzithunzi chochititsa chidwi cha Satana asanachimwe. Akufotokozeredwa ngati mwala wamtengo wapatali. Koma mwala ulibe kuwala kwaokha. Sunyezimira konse mumdima. Kukongola kwake kuli mkuthekera kwake konyezimira pamene waunikidwa ndi kuwala kochokera kunja.

Mulungu atalenga Lusifala, anampatsa kuthekera konyezimira kuonetsera ulemelero wa Mulungu kwakukuru kuposa zolengedwa zonse. Mulungu ndiye kuwala komwe kumapangitsa Lusifala kunyezimira kuonetsa kukongola.

KUGWA KWA SATANA

Satana sanapilire kukhala pa malo okongolawa. Baibulo limafotokozera za kugwa kwake:

Yesaya 14:12-15 Wagwadi kucokera kumwamba, iwe nthanda, mwana wa mbanda kuca! Wagwetsedwa pansu, iwe wolefula amitundu! Ndipo iwe unati mumtima mwako, Ndidzakwera kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wacifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu; ndidzakhala pamwamba pa phiri la khamu,

m'malekezere a kumpoto; ndidzakwera pamwamba pa mitambo, ndidzafanana ndi Wam'mwambamwamba. Koma udzatsitsidwa kungsi ku manda, ku malekezere a dzenje.

Yuda ndi dziko la Israyeli anagulana nawe malonda, anagula malonda ako ndi tirigu wa ku Miniti, ndi zozuna, ndi uci, ndi mafuta, ndi mafuta amankhwala. (Ezekieli 27:17)

Kugwa kwa Satana kuchokera pa malo ake a ulemelero kumwamba kunachitika chifukwa cha kudzikuzana ndi kuukira komwe kunaonekera m'maganizidwe olakwika asanu: Satana anati:

NDIDZAKWERA KUNKA KUMWAMBA: Iye adakhumba kukhala pa malo a Mulungu – Kumwamba – kufuna kufanana ndi Mulungu.

NDIDZAIKA MPANDO WANGA PAMWAMBA PA ANGELO A MULUNGU: Sanangofuna kutenga malo a Mulungu okha komanso ulamulire wake pa angelo onse.

NDIDZAKHALANSO PA PHIRI LA OSONKHANA: Molingana ndi Yesaya 2:2 komanso Masalimo 48:2, awa ndi likulu la ulamuliro wa Mulungu pa dziko lapansi. Satana amafuna kulamulira dziko lapansi komanso angelo.

NDIDZAKWERA PAMWAMBA PA MITAMBO: Mitambo imalankhula za ulemelero wa Mulungu. Satana amafuna ulemelero wa Mulungu kwa Iye yekha. (Mavesi otsatirawa akukamba za mitambo moonetsera ulemelero wa Mulungu: Eksodo 13:21; 40-28-34; Yobu 37-15-16; Mateyu 26:64; Chibvumbulutso 14:14-16).

NDIDZAKHALA NGATI WAM'MWAMBAMWAMBA: Mulungu ali ndi maina ambiri monga taphunzira kale. Nanga chifukwa chiyani Satana anasankha dzina ili? Iye anasankha dzina ili chifukwa limaonetsera Mulungu monga (mwini kumwamba ndi dziko lapansi).

ZOTSATIRA ZA TCHIMO LA SATANA

Zotsatira za tchimo la Satana ndi zoopsa kwambiri ndipo ndi izi:

1. KUCHOTSEDWA KUMWAMBA

Chifukwa cha kugalukira kwake, Mulungu anamchotsa Satana kumwamba:

Mwa kucuruka kwa malonda ako anakudzaza m'kati mwako ndi ciwawa, ndipo unacimwa; cifukwa cace ndinakukankha kukucotsa pa phiri la Mulungu; ndipo ndinakuononga, kerubi wakuphimba iwe, kukucotsa pakati pa miyala yamoto. Unadzikuza mtima cifukwa ca kukongola kwako, waipsa nzeru zako; cifukwa ca kuwala kwako ndakugwetsa pansu, ndakuika pamaso pa mafumu, kuti akupenye. (Ezekieli 28:16-17)

2. KUONONGEKA KWA CHIKHALIDWE

Lucifala, yemwe analengedwa ku ulemelero wa Mulungu, anasanduka kukhala Satana ndi chikhalidwe chotsutsa zonse zomwe Mulungu ali ndi zomwe amachita.

3. KUGWIRITSA NTCHITO MPHAMVU MOLAKWIKWA

Mphamvu za Satana zomwe zinali kugwira ntchito ku ulemelero wa Mulungu. Tsopano ikugwiritsidwa ntchito ndi zolinga zofuna kuononga ndi kusokoneza. Molingana ndi Yesaya 14, Satana amafooketsa maiko (12), amagwedeza dziko lapansi koma maboma (16), ndipo akapolo ake alibe mpumulo (17).

4. ADZAPONYEDWA MNYANJA YA MOTO

Satana anaikidwiritu kuti adzaponyedwa mu nyanja ya moto (Yesaya 14:15).

5. ZINAKHUZA ANGELO ENA A MULUNGU

Pamene Satana anali kugwa kuchoka kumwamba, sanagwe yekha ayi. Anatengako gawo lina la gulu la angelo a kumwamba omwe anatenga nawo mbali pakugalukira Mulungu. Gulu la angelo limeneli tsopani lili mbali imodzi ya mphamvu za kumdima za ziwanda zomwe muphunzire mu chaputala chotsatirachi.

6. KUBWERA KWA TCHIMO KU DZIKO LAPANSI

Pamene Satana anakira Mulungu, tchimo linalowa m'dziko. Chifukwa cha ichi, Mulungu akadatha kuchita zinthu ziwiri izi:

- a. Akadatha kumukantha Satana ndi kumupha. Koma Mulungu akanathana ndi mdani woyamba mu niira iyi, mwayi wokhala ndi mgalukiro wina unali waukulu. Nkhani zochitika kumwamba zikanakhala zowukira Mulungu zokhazokha.
- b. Chinthu china chomwe Mulungu akanachita ndi yomwe anachita molingana ndi zomwe timapeza m'Baibulo. Zomwe Satana amanena kuti ndiwamphamvu zimayenera kutsimikizidwa ngati ndi zoonza mkupita kwa nthawi. Mulungu atalenga mwamuna ndi mkazi woyamba, kutsimikizidwa kwa mphamvu ya Satanaku pa dziko lapansi kunayambika. Mutha kuwerenga nkhani ya kuyesedwa ndi kuchimwa kwa Adam ndi Hava mu Genesis 3.

Muphunzira zambiri za izi mukayamba kusanthula njira za zake za Satana ku tsogoloku.

Nkhondoyi ikadali kuchitika pa dziko lapansi. Ndiye nkondo yauzimuyo. Satana akufunabe mphamvu, udindo ndi kupembedzedwa. Koma kutsogoloku muphunzira kuti iye ndi wogonjetsedwa kale. Yesu anagonjetsa mphamvu za Satana kudzera mu imfa yake komanso kuuka kwake. Tsogolo la Satana linabvumbulutsidwa kale m'Mau a Mulungu.

SATANA ALI KUTI

Satana akupezeka mdzikoli koma mwa uzimu:

Nati Yehova kwa Satana, Ufuma kuti? Nayankha Satana kwa Yehova, nati, Kupitapita m'dziko ndi kuyendayenda m'mwemo. (Yobu 1:7)

Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire: (1 Petro 5:8)

Ngakhale Satana akupezeka pa dziko lapansi iye sali ponseponse. Kutanthauza kuti sangapezeke paliponse nthawi imodzi monga momwe Mulungu alili. Ndi chifukwa chake amatumiza magulu magulu a ziwanda kuti azikwaniritsa ntchito mapulani ake.

MACHITACHITA A SATANA

Satana ali ndi mwayi wopezeka pamaso pa Mulungu ndipo akugwira ntchito pa dziko lapansi komanso mlengalenga:

Ndipo panali tsiku lakuti ana a Mulungu anadza kudzionetsa kwa Yehova, nadzanso Satana pakati pao. Nati Yehova kwa Satana, Ufuma kuti? Nayankha Satana kwa Yehova, nati, Kupitapita m'dziko ndi kuyendayenda m'mwemo. (Yobu 1:6-7)

zimene munayendamo kale, monga mwa mayendedwe a dziko lapansi lino, monga mwa mkulu wa ulamuliro wa mlengalenga, wa mzimu wakucita tsopano mwa ana a kusamvera; (Aefeso 2:2)

Tikhoza kuumba mkota kuti ntchito zonse za Satana podziwa kuti iye nthawi zonse amakhala akulimbana ndi Mulungu, dongosolo lake komanso anthu ake. Alimbana nanu mu dera la kupembedza Mulungu, Mau a Mulungu, moyo wanu wa Chikhristu ndi kutumikira Mulungu kwanu. Tiona ntchito za Satanazi mwatsatane-tsatane m'maphunziro akutsogoloku.

CHIKHALIDWE CHA SATANA

Monga mwaphunzira kale, Satana ndi mzimu, komano ali ndi machitidwe a ngati munthu. Baibulo limamfotokozera motere:

WANZERU NDI WOCHENJERA

Koma ndiopa, kuti pena, monga njoka inanyenga Heva ndi kucenjerera kwace, maganizo anu angaipsidwe kusiyana nako kuona mtima ndi kuyera mtima ziri kwa Kristu. (2 Akorinto 11:3)

AMATHA KUKHUMUDWA KAPENA KUKWIYA

Iye wakukhala nalo khutu amve cimene Mzimu anena kwa Mipingo. Kwa iye wolakika, ndidzampatsa mana obisika, ndipo ndidzampatsa mwala woyera, ndi pa mwalawo dzina latsopano lolembedwapo, wosalidziwa munthu ali yense koma iye wakuulandira. (Cibvumbulutso 2:17)

AMATSIKIZIKA KUCHITA KANTHU

ndipo akadzipulumutse ku msampha wa mdierekezi, m'mene anagwidwa naye, ku cifuniro cace. (2Timoteo 2:26)

WAMPHAMVU

zimene munayendamo kale, monga mwa mayendedwe a dziko lapansi lino, monga mwa mkulu wa ulamuliro wa mlengalenga, wa mzimu wakucita tsopano mwa ana a kusamvera. (Aefeso 2:2)

WOSOCHERETSA

Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi. (Aefeso 6:11)

WOOPSA NDI WANKHAZA

Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire: (1 Petro 5:8)

WONYENGA

Ndipo kulibe kudabwa; pakuti Satana yemwe adzionetsa ngati mngelo wa kuunika. (2 Akorinto 11:14)

MAINA A SATANA

Baibulo lilitipatsa maina ambiri a Satana omwe amafotokozera chikhalidwe ndi machitidwe ake. Monga mwaphunzira kale, Iye asanaukire Mulungu amatchedwa “m’kerubi wodzodzedwa” komanso “Lusifala.” Maina ena a Satana ndi:

Abadoni: (m’Chihebri: Mngelo woononga)	Chibvumbulutso 9:11
Wotsutsa wa abale:	Chibvumbulutso 12:10
Mdani:	1 Petro 5:8
Mngelo wa dzenje lakuya:	Chibvumbulutso 9:11
Mngelo wakuunika:	2 Akorinto 11:4
Apolion (m’Chigriki: woononga):	Chibvumbulutso 9:11
Bezebulu:	Mateyu 12:24; Luka 11:15; Marko 3:22
Beliali:	2 Akorinto 6:15
Wonyenga:	Chibvumbulutso 12:9; 20:3
Woononga:	Chibvumbulutso 9:11; 1 Akorinto 10:10
Mdierekezi: (woipitsa anzake)	1 Petro 5:8; Mateyu 4:1
Chinjoka:	Chibvumbulutso 12:3
Mdani:	Mateyu 13:3

Woipayo:	1 Yohane 5:19
Mulungu wa dziko lapansi:	2 Akorinto 4:4
Mfumu ya ku Turo:	Ezekiel 28:12-15
Wabodza, ndi tate wa abodza:	Yohane 8:44
Wakupha:	Yohane 8:44
Mfumu ya oipa:	Mateyu 12:24
Mfumu ya dziko lapansi:	Yohane 12:31; 14:30; 16:11
Mfumu ya mphamvu ya mlengalenga:	Aefeso 2:2
Satana: (kutanthauza kuti mdani, wotsutsa)	Yohane 13:27
Chinjoka:	Chibvumbulutso 12:9; 2 Akorinto 1:3
Woyesa:	Mateyu 4:3; 1 Atesalonika 3:5
Mkango wobangula:	1 Petro 5:8
Wolamulira wa kumdimba:	Aefeso 6:12
Mzimu womwe ukugwira ntchito mwa ana akusamvera:	Aefeso 2:2

Mutha kuona mphamvu za Satana kudzera mu maina ake komanso zichitochito zake. Chifukwa chakuti Satana ndi mdani wochenjera ndi wa mphamvu, Baibulo likuchenjeza kuti:

Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire. (1 Petro 5:8)

Ndipo musampatse mpata mdierekezi (Aefeso 4:27).

ZOMWE SI ALI:

Mosiyana ndi Mulungu, Satana sadziwa zonse. Akanadziwiratu za tsogolo, sakanalola kuti Yesu afe pamtanda. Akanadziwa kuti imfa ya Yesu ithana ndi mphamvu zake ndi kupereka njira yakuti munthu amasulidwe kotheratu ku mphamvu ya uchimo.

Satana si wamphamvuzonse. Yesu anati mphamvu ya Mulungu yomwe ili mwa inu iposa mphamvu ya Satana. Kwa iwo akukukhulupirira mwa Yesu, Satana ndi mdani wogonjetsedwa kale (Yohane 12: 31). Iye ndi wamphamvu kwa okhawo omwe amachita zofuna zake. Koma mphamvu yake ili panso pa mphamvu ya Mulungu (Yobu 1:10-12) ndipo amatha kugonjetsa wokhulupirira pamene wokhulupirayo afooka ndi kugonjera iye.

Chifukwa chakuti Satana sapezeka paliponse nthawi imodzi ngati Mulungu, amatumiza gulu la angelo padziko lonse lapansi kukachita zofuna zake ndi kukwaniritsa zolinga zake. Muphonzira zambiri za angelo amenewa mu chaputala chikubwerachi.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Kodi Satana anapezeka motani?

3. Kodi pachiyambi Satana anali wotani?

4. Ndi chiani chinachitsa kuti Satana agwe?

5. Kodi zotsatira za tchimo la Satana zinali zotani?

6. Kodi dera lomwe Satana amagwirako ntchito ndi liti?

7. Kodi Satana amachita chiyani?

8. Tchulani zikhalidwe za Satana zomwe mungakumbukire kuchokera mu chaputala chino.

(Mayankho a mafunso awa ali kumapeto a bukhu lino)

MACHITA CHITA A LUSO

1. Onani zomwe Baibulo likukamba za mau a Satana. Mau ake amaonetseratu poyera njira zake. Genesis 3:1, 4, 5; Yobu 1:7-12; Yobu 2:1-6; Mateyu 4:1-11; Luka 4:1-13.
2. Satana amatsutsana ndi Mzimu Woyera m'magwiridwe awo a ntchito. Mzimu anatomizidwa kuti akakokere anthu kwa Mulungu. Satana amagwira ntchito yochotsa anthu pamaso pa Mulungu.

Mzimu Woyera	Satana	Vesi
Mzimu wa Choonadi	Mzimu wonama	1 Yohane 4:6
Wooni	Wabodza	Yohane 14:17; 8:44
Wopereka moyo	Wakupha	1 Akorinto 15:45; Yohane 8:44
Woyera	Woipa	Aroma 1:4; Mateyu 6:13
Ngati nkhunda	Ngati njoka	Mateyu 3:16; Chibvu. 12:9
Mthandizi wathu	Mdani wathu	Aroma 8:26; 1 Petro 5:8
Amalankhulitsa	Amatseka pakamwa	Machitidwe 2:4; Marko 9:17
Wotilankhulira	Wotineneza	Yohane 14:16; Job 1:9-11
Wamphamvu kuposa Satana	Munthu wa mphamvu	Luka 11:21-22

3. Yesu ananena kuti Satana...:
 - Ndi mdani: Mateyu 13:39
 - Ndi woipa: Mateyu 13:38
 - Ndi mfumu ya dziko lapansi: Yohane 12:31; 14:30
 - Ndi wabodza ndi tate wabodza: Yohane 8:44
 - Ndi wakupha: Yohane 8:44
 - Anagwa kuchoka kumwamba: Luka 10:18
 - Ali ndi ufumu: Mateyu 12:26
 - Amafesa nansongole pakati pa tirigu: Mateyu 13:38-39
 - Amalanda mau kwa amene amva: Mateyu 13:19; Marko 4:15; Luka 13:16
 - Anamanga mzimayi kwa zaka 18: Luka 13:16
 - Anakumba kupindula moyo wa Petro: Luke 22:31
 - Ali ndi angelo: Mateyu 25:41
 - Wakonzeredwa moto wosatha: Mateyu 25:41
4. Pamene mumaphunzira phunziro lino la Satana, kodi mwazindikira madera amene mdaniyo akugwiramo ntchito pa moyo wanu? Kodi wakunyengani ndi kukunamizani? Kodi wazembera m'moyo wanu kuti alande mtendere wanu, chimwemwe chanu komanso umboni wanu wa Chikristu? Ndi bwino kudziwa zinthu izi chifukwa madera amene Satana akuchitachita m'moyo wanu ndi ndiye malo a nkhondo yauzimu kwa inu ndipo mugwiritsa ntchito njira zimene muphunzire polimbana naye m'madera amenewo.
5. Satana amayerkezedwa ndi njoka kuthupi. Tanonani momwe mungagwiritsire ntchito mfundo zakuthupi izi mu nkhondo yauzimu:
 Ululu wa njoka umagwira ntchito m'madera awa ukalowa mthupi la munthu:

- a. Mitsempha kapena mphamvu
- b. Magazi
- c. Mtima

Satana nayenso amalimbana ndi mphamvu zanu (mitsempha), kupembedza Mulungu kwanu (mtima), komanso chipulumutso, machiritso, ndi mamasulidwe anu (kutsekereza ntchito ya mwanzi wa Yesu).

Njoka zimaziteteza zokha mu njira izi:

- **Kudzizimbaisa:** Njoka zina zimavuta kuti munthu azizindikire pamene zikabisala popeza zimafana kwambiri ndi pomwe zabisalapo kaya ndi panso kapena mu mtengo.
- **Kutsanzira:** Njoka zina ngati m'bobo umasadzipanga wokha kuoneka ngati nthambi ina ya mtengo posolola khosi lake kuti anthu asaizindikire.
- **Kudzionjezera msinkhu:** Njoka zina monga mamba imadziteteza yokha podzifufumitsa kwambiri.
- **Kulira moopseza:** Njoka zina zimalira moopseza kwambiri kuti anthu achite mantha ndi kuthawa.

Chimodzimodzinso mdani wanu wauzimu amadzizimbaisa, kutengera ntchito za Mulungu ndi kukuopsezani podzifufumitsa ndi kulira moopseza.

Njoka zimagwira zakudya zawo mu njira zinayi zosiyana:

- a. Kudumphira: imadumphira mwachangu kwambiri ndi kuluma kapena kugwira chinthu.
- b. Kukulunga: Apa ndi pomwe njokayo imakulunga chinthu chomwe yagwira ndi kuifinya mpaka itafa.
- c. Kupsinja: Njoka imathanso kupsinja chinthu chomwe yagwira ndipo chifukwa cha kulemera kwake chinthu chija chimakanika kudzipulumutsa mpaka kufa.
- d. Kuluma: Imatha kuluma chinthu osachotsa mano ake msanga kufikira itafinyira ululu wake wonse mwa chinthu chomwe yagwira mpaka kufooka ndi kufa.

Nthawi zina mano ake amathyokera pa chomwe inagwiracho, koma amaphukiranso mosavuta. Pa thupi lonse la njoka, kamwa ndiye yoopsa kwambiri. Imaluma ndi kulavula ululu woopsa kwambiri womwe umafooketsa ndikupha chomwe ikufuna kudya.

Mukutha kuona kufanana pakati pa zomwe njoka imachita ndi momwe Satana amagwirira ntchito? Nthawi zina amadumphira munthu mwachangu kwambiri ndi kumupha pomwepo. Nthawi zina amangokulunga moyo wauzimu wa munthu ndi zokoma za dziko komanso zolemetsa zauchimo. Amayesetsa kupsinja anthu ndi kuwapanikiza kuti asataketake. Ndipo amakonda kugwira munthu mu ukapolo wa tchimo ndi kumulavulira ululu womwe umadzaononga moyo wake.

Njoka imadziwa kuti pali munthu kapena chinthu, pamene fumbi langwera pa lilime lake kenako uthenga umafika ku ubongo za komwe chakudya chili. Ngati munthu atangoima chilili, njoka siingadziwe pomwe ali. Satana amadziwa pomwe munthu ali chifukwa cha fumbi lomwe limachitika pamene iye wasokonezeka ndi kuthamangathamanga chifukwa cha mantha. Fumbi

likakhala bata, iwe nuima chilili kukumana naye mopanda mantha, m'mene njoka imachitira, sangakuchite kanthu. Ichi ndi chifukwa chake Baibulo limati: “khala chete” kapena “imanibe.”

Njoka ikapanikizika, imatha kulavula ululu wake wonse nthawi imodzi, ndipo ikatero imakhala yopanda mphamvu kwa kanthawi kufikira thupi lake litapanganso ululu wina. Mwina nchifukwa chake pamene Yesu anagonjetsa Satana m'chipululu nthawi ya kuyesedwa, Baibulo limati, “ndipo anamchokera Iye kwa kanthawi.”

Zina mwa njira zopewera kulumidwa ndi njoka kuthupi nazi. Mukaonesetsa mupeza kuti zikugwirizana ndi njira zauzimu:

1. Muyenera kudziwa mtundu wa njoka zoopsa (kudziwa mdani wako).
2. Bvalani zovala zodzitetezera (zida zanu za nkhondo yauzimu).
3. Pewani kupita malo odziwikiratu kuti kumakhala njoka (osamapita ku malo komwe kukuchitika zoipa kapena komwe mungayesedwe)
4. Mukhale ndi mnzanu (kufunika kokhala membala wa mpingo).
5. Pewani kuyenda kutada kapena malo amdima. Njoka zimapewa kuwala kwa dzuwa. (monga okhulupirira sitiyenda monga ana amdima koma ngati ana akuunika).
6. Osaika phazi kapena dzanja lanu pa malo omwe simungathe kuona bwino bwino (samalani ndi zokhumba zathupi).
7. Osakhala pansu musanaonesetse bwino bwino pomwe mukukhalapo (chinthu chokhazikika sichivuta kugenda kusiyana ndi chomwe chikuyendayenda).
8. Osapita kosakasaka njoka kuti mukaphe. Anthu ambiri amalumidwa chaka ndi chaka chifukwa amayesayesa kuti aphe njoka asakudziwa chikhalidwe cha njokazo kapena malo omwe zimakhala. (Timankaniza woipayo tikakumana naye osati kukamusaka-saka ayi).

Munthu akalumidwa ndi njoka, timatema malo omwe walumidwawo ngati tikujambula mtanda (+) ndi kuyamwa ululu wonse. Kodi umu si momwe Khristu anatimasulira ife ku ululu wa tchimo kudzera mu imfa yake ya pamtanda?

Tili ndi mphamvu pa njoka. Mu Genesis 3, Mulungu analankhula thembelero pa njoka (Satana). Anati mutu wake udzaphwanyidwa ndi mbeu yamkazi (Yesu) ndipo chitendeni cha mbeu (Yesu) chidzavulazidwa ndi njoka.

“Kuvulazidwa” kwa “chitendeni” cha Yesu ndi chinzunzo chomwe Yesu anadutsamo pophwaya mutu wa Satana pa mtanda. Yesu ataphwaya mutu wa Satana, zinali ngati kudula mutu wa njoka ya ululu kuthupi. Komabe mutu umenewu umatha kukhala maola anayi udakali woopsa kuti ukhoza kuluma munthu. Zimamveka kuti mtima wa njoka yodulidwa mutuyi umatha kumagundabe mpaka masiku awiri ndipo thupi lonse limakhala likusunthasuntha.

Yesu anadula mutu wa “njoka” pa mtanda, koma njokayo ikadali moyo. Satana akuchitachitabe mdziko kufikira tsopano lino ndipo adakali wamphamvu. Komabe alibe ulamuliro. Ulamuliro

womwe angakhale nawo pa moyo wanu ndi womwe inu mwampatsa ndipo mphamvu ya ndi ulamuliro zomwe zili mwa inu (Yesu) ndizoposa mphamvu zake kutali-tali.

CHAPUTALA 6

MPHAMVU ZA KUMDIMA: ZIWANDA

ZOLINGA

Pa mapeto pa chaputala chino mukuyenera kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kukumbukira chiyambi cha ziwanda
- Kufotokozerana zomwe ziwanda zinali poyamba
- Kuzindikira dera lomwe ziwanda zimagwira ntchito
- Kuzindikira chikhalidwe cha ziwanda
- Kufotokozerana dongosolo la mphamvu za ziwanda
- Kuumba mkota pa ntchito za ziwanda

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m' masiku otsiriza ena adzataya cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunzira a ziwanda, (1 Timoteo 4:1)

MAU OTSOGOLERA

Mu chaputala chapitachi mwaphunzira za Satana. Mu chaputala chino muphunzira zagulu lake la nkhondo lotchedwa ziwanda lomwe iye amaliramulira. Anthu ena salabadira konse kuphunzira za ziwanda. Ena ali ndi chidwi choonjeza pa phunziroli. Sitikuyenera kuchepa mphamvu ya mizimu yoipa ya ziwanda pa dziko lapansi komanso tibatengeke nazo kwambiri kufika pa mlingo womangoona chiwanda mu chirichonse chochitika ndi mwa wina aliyense yemwe ali pafupi nanu. Phunzirani za ziwanda monga momwe Baibulo limafotokozerana ndipo musawerenge mabuku achikunja pofuna kumvetsa za mphamvu za kumdima. Gwiritsani ntchito Baibulo kapena mabuku abwino a Chikristu.

CHIYAMBI CHA ZIWANDA

Mulungu ndi amene analenga angelo onse, ena anagwa ndipo anasanduka ziwanda:

Zonse: zinalengedwa ndi iye; ndipo kopanda iye sikunalengedwa kanthu kali konse kolengedwa, (Yohane 1:3)

pakuti mwa iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yacifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa iye ndi kwa iye. (Akolose 1:16)

CHIYAMBI NDI KUGWA KWA ZIWANDA

Poyamba ziwanda zinali monga ngati angelo onse omwe Mulungu adalenga. Anali ndi malo komanso ntchito zofanana ndi angelo abwino momwe mwaonera kale mu chaputala 4 cha phunziro lino. Satana atakira Mulungu, gawo lina la angelo linatenga nawo mbali. Ndipo Mulungu anawachotsa kumwamba pamodzi ndi Satana. Zitatero sanakhalenso angelo koma anasanduka ziwanda:

Ndipo munali nkondo m'mwamba. Mikayeli ndi angelo ace akucita nkondo ndi cinjoka; cinjokanso ndi angelo ace cinacita nkondo; ndipo sicinalakika, ndipo sanapezekanso malo ao m'mwamba. Ndipo cinaponyedwa pansu cinjoka cacikuru, njoka yokalambayo, iye wochedwa mdierekezi ndi Satana, wonyanga wa dziko lonse; cinaponyedwa pansu kudziko, ndi angelo ace anaponyedwa naye pamodzi. (Cibvumbulutso 12:7-9)

Ngati ziwanda si angelo omwe anagwa, ndiye kuti tilibenso kufotozera kwina molingana ndi Baibulo za komwe ziwanda zinachokera. Satana sangadzilengere yekha gulu lake la nkondo popeza zinthu zonse zinalengedwa ndi Mulungu. Pali magulu awiri angelo akugwawa. Gulu lina limatsutsa Mulungu ndi anthu ake pa dziko lapansi ndipo lina lamangidwa ndi maunyolo:

Pakuti ngati Mulungu sanalekerera angelo adacimwawo, koma anawaponya kundende nawaika ku maenje a mdima, asungike akaweruzidwe. (2 Petro 2:4)

Angelonso amene sanasunga cikhalidwe cao coyamba, komatu anasiya pokhala pao pao, adawasunga m'ndende zosatha pansu pa mdima, kufikira ciweruziro ca tsiku lalikuru. (Yuda 1:6)

Pali angelo ochitachita ndi angelo omangidwa. Mtsogoleri wa magulu onsewa ndi Satana, yemwe amatchedwa “mfumu” ya mizimu yoipa (Mateyu 12:24). Gahena anakonzeredwa Satana ndi angelo ake, ndiye malo awo omaliza:

Pomwepo Iye adzanena kwa iwo a ku dzanja lamanzere, Cokani kwa Ine otembereredwa inu, ku mota wa nthawi zonse wokolezedwera mdierekezi ndi amithenga ace: (Mateyu 25:41)

Pamene Yesu anakumana ndi amuna awiri odzadzidwa ndi ziwanda, yankho lawo linali lakuti:

Ndipo pofika Iye ku tsidya lina, ku dziko la Agadara, anakumana naye awiri ogwidwa ndi ziwanda, akuturuka kumanda, aukali ndithu, kotero kuti sangathe kupitapa munthu pa njira imeneyo. (Mateyu 8:28)

Ziwanda zomwe zinali mwa amuna awiriwa zimadziwa bwino lomwe kuti malo awo omaliza ndi ku chizunzo chosatha. Popeza Gahena ndi malo a chizunzo ndipo anakonzeredwa Satana pamodzi ndi angelo ake, ndiye kuti ziwanda ndi angelo omwe anagwa pamodzi naye.

DERA LOMWE ZIWANDA ZIMAGWIRA NTCHITO

M’Baibulo lonse, timapeza kuti ziwanda zikuchita-chita pa dziko lapansi. Popeza Satana sapezeka paliponse nthawi imodzi, amagwiritsa ntchito ziwanda kukachita chifuniro chake ndi kukwaniritsa zolinga zake pa dziko lonse lapansi. Ndiye aja amatchedwa kuti “mphamvu za mlengalenga” (Aefeso 2:2) komanso “mphamvu za mdima” ndipo onse panso pa ulamuliro wa Satana.

CHIKHALIDWE CHA ZIWANDA

Zisanachimwe ziwanda zinali ndi makhalidwe ofanana ndi angelo abwino monga taonera kale. Koma tsopano ziwandazi:

Ndi mizimu:	Mateyu 8:16; Luka 10:17, 20
Zitha kuonekera:	Genesis 3:1; Zekariya 3:1; Mateyu 4:9-10
Zitha kulankhula:	Marko 5:9, 12; Luka 8:28; Mateyu 8:31
Zimakhulupilira:	Yakobo 2:19
Zimatha kuchita zomwe zikufuna:	Luka 11:24; 8:32
Zimaonetsera nzeru:	Marko 1:24
Zimatha kukwiya/kukhumudwa:	Luka 8:28; Yakobo 2:19
Zimatha kuzindikira:	Machitidwe 19:15
Zili ndi mphamvu zoposa:	Machitidwe 19:16; Marko 5:3
Zimatha kuonekera mwa mphamvu:	Daniel 9:21-23
Ndi zosafa:	Mateyu 25:41
Ziri ndi chiphunzitsa:	1 Timoteyo 4:1-3
Ndizoipa:	Mateyu 10:1; Marko 1:27; 3:11

MAINA A ZIWANDA

Ziwanda zatchulidwa “mizimu yoipa” kasanu ndi kamodzi ndipo yatchulidwa “mizimu yonyansa” maulendo okwana 23 mu Chipangano Chatsopano. Zimatchedwanso “ziwanda” (Marko 1:32) komanso “angelo a Satana” (Mateyu 25:41).

DONGOSOLO LA ZIWANDA

Tiyeni tionenso momwe Mulungu anakonzera dongosolo la gulu la angelo ake:

**pakuti mwa iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yacifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa iye ndi kwa iye.
(Akolose 1:16)**

Satana satha kupanga zake, amangotengera. Wakonza dongosolo la ziwanda zake mofanana ndi momwe Mulungu anachitira.

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

Satana waika mphamvu zake mu:

Maukulu: Satana zimaonetsa kuti anagawa dzikoli m' maukulu. Awa ndi madera omwe amakhala ndi mfumu yolamulira. Ndipo Satana waika mfumu yolamulira mu ukulu wina uliwonse. Mfumu ya mphamvu ya Perezi yatchulidwa mu Daniel 10. Umu ndi m'mene Satana amagwilira ntchito kulamulira maiko ndi maboma.

Mphamvu ndi maulamuliro a mdima a dziko lino: Magawo awiri a ziwanda awa amagwira kulamulira dongosolo la umoyo wa anthu, zandale ndi zachikhalidwe pa dziko lapansi. Muphunzirabe za momwe mungathanirane ndi mphamvu za maukuluzi mukamadzaphunzira za ndondomeko zauzimu zogonjetsera dziko lapansi mukafika mu chaputala 14.

Auzimu a choipa a malo okwera: Malo okwera m'Chipangano Chakale anali ochitira chipembedzo. Umu ndi momwe Satana amagwirira ntchito mu ndondomeko za chipembedzo za dziko lapansi. Muphunzira zambiri za izi mu chaputala 20 mukamadzaphunzira za zoipa zauzimu m'malo okwera.

Magulu atatu taonawa amasiyana makulidwe. Mwachitsanzo, Maria Magdalena anali ndi ziwanda zisanu ndi ziwiri pamene amamasulidwa. Mu Luka 8:30 timamva za “legio” ya ziwanda. Ili ndi gulu la asilikali a Chiroma okwana 6100 kapena 726 a pangamira.

Mphamvu za ziwanda zomwe zagawidwazi:

Ndi zogwirizana:

Mu nkhani ya munthu wogwidwa ndi ziwanda pa Luka 8:30 tikuona kuti ziwandazi zinali zogwirizana mu cholinga chawo, chomwe chinali kuzunza munthuyu. Chimodzimodzinso mu Mateyu 12:45 ndi nkhani ya Maria Magdalena yemwe anali ndi ziwanda zisanu ndi ziwiri (Luka 16:9). Yesu analankhulapo za mgwirizano wa mphamvu ya ziwanda ponena kuti:

ndipo ngati Satana amaturutsa Satana, iye agawanika pa yekha; ndipo udzakhala bwanji ufumu wace? (Mateyu 12:26)

Kuipa kwao ndi kosiyana milingo:

Izi zafotokozedwa ndi chiwanda chomwe chinanena kuti chikabweranso ndi ziwanda zina zoipa kwambiri:

Koma mzimu wonyansa, utaturuka mwa munthu, umapitirira malo opanda madzi kufunafuna mpumulo, osaupeza. Pomwepo unena, ndidzabwerera kunka kunyumba kwanga, konkuja ndinaturukako; ndipo pakufikako uipeza yopanda wokhalamo, yosessedwa ndi yokonzedwa. Pomwepo upita, nutenga pamodzi ndi uwu

mizimu yina inzace isanu ndi iwiri yoipa yoposa mwini yekhayo, ndipo ilowa, nikhalamo. Ndipo 4 matsirizidwe ace a munthu uyo akhala oipa oposa mayambidwe ace. Kotero kudzakhalanso kwa obadwa oipa amakono. (Mateyu 12:43-45)

Zimasintha ntchito zawo:

Chiwanda cha pa 1 Mafumu 22:21-23 chinanena kuti chikhala mzimu wabodza. Kuonetsa kuti sichinali choncho poyamba popeza chinanena kuti “Ndikhala...”

Ndi za mitundu yosiyana-siyana:

Baibulo limaphunzitsa kuti munthu ali ndi thupi, moyo ndi mzimu. Palinso mitundu itatu ya ziwanda yomwe imalowa m’thupi, m’moyo, ndi m’mzimu wa munthu:

1. Mizimu yoipa kapena yonyansa: Imapitsa patsogolo m’chitidwe wa chiwerewere, maganizo onyansa, kupondereza, kuzunza anthu, kukhumudwa kopilira muyezo ndi njira zina zambiri zomwe muphunzirebe patsogolopa. Zimalowa ndi kusautsa maganizo ndi moyo wa munthu (Mateyu 10:1; 12:43; Marko 1:23-26).
2. Mizimu ya matenda: zimasautsa thupi la munthu (Luka 13:11).
3. Mizimu yonyenga: Imasautsa maganizo, moyo, ndi mzimu kumpanga munthu kuti ayambe kukhulupilira ziphunzitsa zonyenga (1 Timoteyu 4:1). Mizimu iyi imanyenga anthu kuti akhulupirire bodza ndipo kuti apite ku chionongeko chamuyaya. Ndi mizimu ya ziphunzitsa zonyenga, mafano, a Khristu abodza ndi aphunzitsi onama.

MACHITACHITA A ZIWANDA

Ziwanda zimatsatira malamulo operekedwa ndi mfumu yawo, Satana. Tingathe kunena mwachidule kuti ntchito ya ziwanda ndiko kutsutsa Mulungu, dongosolo lake komanso anthu ake. Ziwanda zimagwiritsidwa ntchito ndi Satana kulimbana ndi Mau a Mulungu, kupembedza kwanu Mulungu, ubale wanu ndi Mulungu, ndi kutumikira kwanu Mulungu.

Mu chaputala 8 muphunzira tsatane-tsatane wa ndondomeko za mdaniyo mu nkondo yauzimu. Satana amagwiritsa ntchito ziwanda kuti akwaniritse ndondomeko yake pa dziko lapansi. Ziwanda zimakuza mphamvu za Satana popititsa patsogolo chinyengo ndi moyo wauchimo. Amalimbana ndi anthu paokha, maiko, maboma komanso ndondomeko za dziko. Amaipitsa Mulungu ndi anthu ake. Zimapititsa patsogolo kupembedza mafano, ziphunzitsa zonyenga, kuphimba anthu kuti asaone choonadi cha Uthenga Wabwino.

Ziwanda zimathana ndi osakhulupirira powapangitsa kuti azichita zoopsa, kupha, kuvulaza, komanso kudzipha okha ndi zina zambiri. Zimasokoneka maganizo a anthu ndi mavuto osiyana-siyana komanso matenda mthupi. Zimalimbana ndi okhulupirira kudzera m’mayesero, chinyengo, kusowa mtendere ndi chizunzo. Zimayesetsa kuika anthu mu ukapolo wa zizolowezi zoipa ndi mantha. Zimatsutsa ndi kukuipitsini komanso kubweretsa magawano pakati pa anthu a Mulungu. Zimafuna kusokoneza ubale wanu ndi Mulungu, kupembedza kwanu ndi utumiki wanu. Zimalimbananso ndi thupi lanu.

Anthu osakhulupirira amakhala opanda chitetezo ku mivi ya mphamvu za ziwanda, koma okhulupirira ali ndi zida zauzimu za mphamvu ndi ndondomeko zolimbana ndi mphamvu zakumdima. Muphunzira za zida komanso ndondomeko pamene mupitiriza kuphunzira za nkhondo yauzimu.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Kodi ziwanda zinayamba bwanji?

3. Kodi dera lomwe zimagwira ntchito ndi liti?

4. Lembani mwachidule ntchito za ziwanda.

5. Lembani za chikhalidwe cha ziwanda momwe mungakwanitsire kukumbukira.

6. Kodi mphamvu za ziwanda zaikidwa mu dongosolo lotani?

7. Kodi poyamba ziwanda zinali zotani zisanagalukire Mulungu?

8. Chifukwa chiyani zinakhala ziwanda?

9. Perekani tanthauzo lachidule la mau ali m'musimu:

Maulamuliro:

Mphamvu ndi olamulira:

Zoipa zauzimu m'zakumwa:

(Mayankho a mayesowa ali ku mapeto a buku lino).

MACHITA-CHITA ALUSO

1. Kuti muphunzire zambiri za mphamvu za kumdima, werengani mavesi ali m'musiwa pa mutu wa ziwanda:

Genesis: 3:1-15; 6:1-4; 41:8; 44:5

Eksodo: 7:8-13; 20-24; 8:6-7, 18-19; 9:11; 22:18

Levitiko: 17:7; 19:26,31; 20:6,27

Numeri: 22:7; 23:23

Deuteronomu: 18:9-14, 20-22; 32:17

Oweruza: 8:21,26

1 Samuel: 15:23; 16:14; 18:10; 28:1-15

1 Mafumu: 5:4; 18:28; 22:19-38

2 Mafumu: 9:22; 17:17; 21:1-9; 23:5,24

1 Mbiri: 21:1

2 Mbiri: 33:1-10

Yobu: 1:1-12; 2:1

Masalimo: 78:49; 91:6; 106:36-38

Yesaya: 3:18-19; 8:19; 14:12-17; 47:11-15

Yeremiya: 27:9

Ezekiel: 21:21; 28:11-19

Daniel: 1:20; 2:2,27; 4:6-9; 5:7, 11, 15

Hoseya: 4:12

Mika: 5:12

Zakariya: 3:1,2; 10:2

Malaki: 3:5

Mateyu: 4:1-11, 24; 8:16, 28-34; 9:32-34; 10:1, 25; 11:18; 12:22-30, 11:43-45; 13:19,

39: 15:21-28; 17:14-21; 24:24; 25:41

Marko: 1:12-13, 21-28, 32, 34, 39; 3:11-12, 15, 22-30; 5:1-20; 6:7, 13; 7:24-30; 8:33; 9:17-29, 38-40; 13:22; 16:9, 17

Luka: 4:1-13, 33-37; 6:18; 7:21,33; 8:2, 26-39; 9:1, 37-42, 49-50; 10:17-20; 11:14-26; 13:10-17, 32; 22:3, 31; 24:39

Yohane: 6:70; 7:20; 8:44, 48-49; 10:20-21; 12:31; 13:27; 14:30; 16:11; 17:15

Machitidwe: 5:3, 16; 8:7, 9-11, 18:24; 10:38; 13:6-12; 16:16-19; 19:12-20; 26:18

Aroma: 8:38-39; 16:20

1 Akorinto: 5:5; 7:5; 10:20-21

2 Akorinto: 2:11; 4:4, 6:14, 15, 17; 11:13-14; 12:7

Agalatiya: 1:4; 3:1; 4:8-9; 5:19-21

Aefeso: 1:21; 2:2; 4:26-27; 6:11, 12, 16

Akolose: 1:13; 2:15

Atesalonika: 2:18; 3:5

2 Atesalonika: 2:1-10; 3:3

1 Timoteyo: 1:20; 3:6; 4:1-3

2 Timoteyo: 1:7; 2:26; 4:18

Ahebri: 2:14

Yakobo: 2:19; 3:15; 4:7

1 Petro: 5:8

2 Petro: 2:4, 19

1 Yohane: 2:13, 18; 3:8, 12; 4:1-4, 6; 5:18

Yuda: 1:6, 9

Chibvumbulutso: 2:9, 13, 24; 3:9; 9:1-11, 20-21; 12:1-13; 13:1-18; 16:13-16; 18:2; 19:20;

20:1-14; 21:8

2. Werengani zomwe Chipangano Chakale chikulemba zokhuza ziwanda:

Satana watchulidwa ngati njoka kasanu ndi kawiri mu Genesisi 3:1-24 ndi Yesaya 27:1.

Satana watchulidwanso mu 1 Mbiri 21:1; 2 Samuel 24:1; Masalimo 109:6; Zakariya 3:1-2; ndi ka khumi ndi kanayi m' buku la Yobu.

Mizimu yoipa yatchulidwa kasanu ndi katatu mu nkhani ya Mfumu Sauli: 1 Samuel 16:14-23; 18:10; 19:9.

Mizimu yabodza yatchulidwa kasanu ndi kamodzi mu 1 Mafumu 22:21-23

Mizimu ya chizolowezi yatchulidwa kasanu ndi kamodzi mu Levitiko 20:27 ndi 1 Samuel 28.

Mizimu ya chipembedzo ndi ya chigololo ikupezeka mu bukhu la Hoseya.

Ziwanda zatengedwa monga milungu ya maiko a chikunja kanayi: Levitiko 17:7;

Deuteronomu 32:17; 2 Mbiri 11:15; Masalimo 106:19-39.

Mafumu oipa olamulira maiko amapezekanso mu Masalimo, mabuku a aneneri, makamakanso mu Daniel 10:10-21.

Mizimu yonyansa yosocheretsa yatchulidwa kawiri: Yesaya 19:14.

3. Talingalirani ichi: Pamene mphamvu za ziwanda ziri pa udani ndi Mulungu, izo

zimagonjera ku chifuniro chake komanso Mulungu amatha kuzigwiritsa ntchito kuti zionongane zokha-zokha. Onani 1 Samuel 16:14;

18:10; 19:9; 1 Mafumu 22:20-22; and Yesaya 19:14.

CHAPUTALA 7 DERA LA MDANI

ZOLINGA:

Mukamaliza phunziro lino mukhala mukukwanitsa kuchita izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kumasulira mau oti “dziko” monga m’mene tagwiritsira ntchito mu phunziro lino.
- Kuzindikira mfumu ya dziko lapansi
- Kupereka chifukwa chokhalira ndi machitidwe a dziko omwe tili nawo lero.
- Kufotokozero momwe dziko limaonera okhulupirira
- Kutanthauzira mau oti “thupi” molingana ndi momwe tagwiritsira ntchito mu phunziro lino.
- Kufotokoza tanthauzo la mau oti “chilakolako cha thupi”
- Kufotokozero momwe chilakolako choipa chimayambira.
- Kufotokoza zotsatira za chilakolako chomwe sichinagonjetsedwe.
- Kudziwa mavesi omwe amakamba za ntchito za thupi.

MAVESI OTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko apansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, cikondi ca Atate Isiciri mwa iye. Pakuti ciri conse ca m'dziko lapansi, cilakolakoca thupi ndi cilakolako ca maso, matamandidwe a moyo, sizicokera kwa Atate, koma ku dziko lapansi. (1 Yohane 2:15-16)

MAU OYAMBA

Pali mdani m’modzi, koma monga mwaphunzira kale amagwiritsa ntchito mphamvu zazikulu za ziwanda ndipo amagwiranso ntchito kudzera mu mphamvu za kumdima za thupi ndi dziko:

Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko apansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, cikondi ca Atate Isiciri mwa iye. Pakuti ciri conse ca m'dziko lapansi, cilakolakoca thupi ndi cilakolako ca maso, matamandidwe a moyo, sizicokera kwa Atate, koma ku dziko lapansi. (1 Yohane 2:15-16)

Cholinga cha chaputala chino ndi kudziwa ndi kusanthula mphamvu zakumdima za Satana zotchedwa dziko ndi thupi. Chenjerani! Mukulowa m’dera losanyengelera munthu. Dziko ndi thupi ndi dera la mdani.

CHIGAWO CHOYAMBA: DZIKO

Mau oti thupi ali ndi matanthauzo osiyana-siyana m’Baibulo. Pena amanthauza nthaka kapena dziko monga m’mene Mulungu analingera. Penanso amanthauza Amitundu omwe ndi mitundu yonse ya dziko lapansi kupatula Ayuda.

Mau oti “dziko” amagwiritsidwanso ntchito pofuna kulankhula za moyo wachikunja womwe anthu amakhala wosemphana ndi Mulungu. Ndi machita-chita omwe akugwiritsidwa ntchito kuyendetsa dziko lokhalamo anthu, omwe ndi osemphana ndi Mulungu ndi Ambuye Yesu Khristu. Tanthauzo ili ndi lomwe tikugwiritsa ntchito mu phunziro lino. “Dziko” ndi gulu la anthu omwe amachita zakuthupi napanga mtundu. Tikati “thupi” apapa sitikutanthauza thupi leni-leni lokhala ndi ziwalo mutu, miyendo ayi. Koma ndi mau omwe amafotokozera chikhalidwe choipa cha mtundu wa anthu chomwe chikuukira Mulugu mwadala.

Dziko, monga mdani wanu, ndi nzeru zokhazikitsidwa zoyendetsera umoyo wa anthu, zachuma komanso chipemphezo. Si boma lina lake, kapena bungwe kapena munthu ayi, koma maziko omwe mabomawo, mabungwewo kapena anthuwo akhazikikapo. Dongosolo limeneli ndi kusefukira kwa chikhalidwe chauchimo pakati pa anthu. Limapititsa patsogolo uchimo pomuzungulira ndi zinthu zofuna kudzutsa zilako-lako za thupi.

MFUMU YA DZIKO LAPANSI

Satana ndi “mfumu” kapena wolamulira wa dongosolo la dziko lapansi:

Tsopano pali kuweruza kwa dziko ili lapansi; mkulu wa dziko ili lapansi adzatayidwa kunja tsopano, (Yohane 12:31).

Sindidzalankhulanso zambiri ndi inu, pakuti 9 mkuru wa dziko lapansi adza; ndipo alibe kanthu mwa Ine; (Yohane 14:30)

Satana amatchedwanso mulungu wa dziko lapansi:

mwa amene mulungu wa nthawi yino ya pansi pano unacititsa khungu maganizo ao a osakhulupirira, kuti ciwalitsiro ca Uthenga Wabwino wa ulemerero wa Kristu, amene ali cithunzithunzi ca Mulungu, cisawawalire. (2 Akorinto 4:4).

Maufumu a dziko lapansi amachita zinthu motsogozedwa ndi Satana. Amayendetsedwa ndi nzeru ndi mfundo zochokera kwa Satana zomwe zimatsindika kwambiri zofuna za thupi:

Pomwensu mdierekezi anamuka naye ku phiri lalitari, namuonetsa maiko onse a dziko lapansi, ndi ulemerero wao; nati kwa Iye, Zonse ndikupatsani Inu, ngati mudzagwa pansi ndi kundigwadira ine. (Mateyu 4:8-9).

Tsiku lina adzakhala maufumu a Ambuye wathu:

Ndipo wina akafuna kuipsa izo, moto uturuka m'kamwa mwao, nuononga adani ao; ndipo wina akafuna kuipsa izo, maphedwe ace ayenera kutero. (Chibvumbulutso 11:5).

TSINDE LA MOMWE ZINTHU ZILIRI PADZIKO LERO

Uchimo ndiye tsinde la momwe zinthu ziliri padziko lero. Adamu ndi Hava atalengedwa ndi Mulungu, anapatsidwa ulamuliro wa pa dziko lons lapansi. Kutanthauza kuti anali ndi mphamvu

zolamulira dziko lonse lapansi, kuliwendetsa molingana dongosolo la Mulungu. Atachimwa pamaso pa Mulungu, ulamulirowu unawachokera (Genesisi 1-3).

Yesu atapachikidwa chifukwa cha machimo a mtundu wa anthu nauka kwa akufa, anatenganso ulamuliro wa pa dziko uja. Ndipo analengeza chiweruzo pa mphamvu zonse za kumdima:

Atabvula maukulu ndi maulamuliro, anawaonetsera poyera, nawagonjetsera nako. (Akolose 2:15).

Koma ngakhale Yesu anatenganso dziko lapansi kuchokera ku ulamuliro wa mdani, Satana sakufunabe kuvomereza. Iye adakagwirabe ntchito pa dziko lapansi ndi mphamvu za kumdima. Iye sadzavomera kuti Yesu ndiye Mfumumu ya maufumu a dziko lapansi kufikira pamene adzagonjetsedwe kotheratu pa nkondo yomaliza. Muphonzira za nkondo imeneyi mu chaputala chomaliza cha buku lino.

Izi ziri ngati momwe zimakhala pa kulimbana kwa boma lolamula ndi zigawenga. Zigawenga sizimavomereza ulamuliro wa boma ndipo amakhala akulimbana nawo kuti alande dziko lomwe silawo nazunza mzika za dzikolo. Amachita izi koma mwa luntha kwambiri kuti zolinga zawo zikwaniritsidwe.

Chimodzimodzi ku dziko lauzimu. Yesu analanda ulamuliro wa dziko lonse lapansi, mdaniyo ndi mphamvu zake za kumdima. Koma gulu lowukira la Satana limamenyabe nkondo mdziko lonse. Amafuna kutenga dziko lomwe silawo konse ndi kutsogolera amuna ndi akazi kuchita zoipa. Nkondo iyi, yomwe ndi nkondo yathu yauzimu ikhala ikupitirirabe kufikira nkondo yomaliza.

MOMWE MPHAMVU ZA DZIKO ZAIKIDWIRA

Dongosolo la dziko laikidwa motsutsana ndi Mulungu, mapulani ake, zolinga zake komanso anthu ake:

Dongosolo Loipa La Dziko

Dongosolo la dziko lero ndi loipa:

amene anadzipereka yekha cifukwa ca macimo athu, kuti akatilanditse ife m'nyengo ya pansu pano yino yoipa, monga mwa cifuniro ca Mulungu ndi Atate wathu;(Agalatiya 1:4).

Dongosolo la dziko ndi lopanda Mulungu:

kuti nthawi ija munali opanda Kristu, alendo a padera ndi mbumba ya Israyeli, ndi alendo alibe kanthu ndi mapangano a malonjezano, opanda ciyembekezo, ndi opanda Mulungu m'dziko lapansi. (Aefeso 2:12).

Pali chinyengo chambiri pa dziko kukopa okhulupirira kuti atenge nawo mbali m'moyo wa dziko.

Pakuti onyenga ambiri adaturuka kulowa m'dziko lapansi, ndiwo amene sabvomereza kuti Yesu Kristu anadza m'thupi, Ameneyo ndiye wonyenga ndi wokana Kristu. (2 Yohane 7).

Dziko laweruzidwa kale ndipo liri panso pa mkwiyo wa Mulungu:

Koma poweruzidwa, tilangidwa ndi Ambuye, kuti tingatsutsidwe pamodzi ndi dziko lapansi. (1 Akorinto 11:32).

Mfundo za Dziko Lapansi:

Izi ndi mfundo zomwe zimayendetsa dziko lapansi. Zimalitsogolora kunka ku chionongeko:

ife, pamene tinali akhanda, tinali akapolo akumvera miyambo ya dziko lapansi; (Agalatiya 4:3).

Maziko a Dziko Lapansi:

Awa ndi malamulo omwe ali maziko a dongosolo la dziko. Ndi osiyana ndi malamulo kapena mfundo zomwe Mulungu wakhazikitsapo Ufumu wake:

Penyani kuti pasakhale wina wakulanda inu ngati cuma, mwa kukonda nzeru kwace, ndi cinyengo copanda pace, potsata mwambo wa anthu, potsata zoyamba za dziko lapansi, osati potsata Kristu; Ngati munafa pamodzi ndi Kristu kusiyana nazo zoyambaza dziko lapansi, mugonieranii ku zoikikazo, monga ngati moyo wanu mukhala nao m'dziko lapansi, (Akolose 2:8, 20).

Mzimu Wa Dziko:

Mzimu wa dziko umatsutsana ndi Mzimu Woyera:

Koma sitinalandira ife mzimu wa dziko lapansi, koma Mzimu wa kwa Mulungu, kuti tikadziwe zimene zipatsidwa kwa ife ndi Mulungu kwaufulu. (1 Akorinto 2:12).

Gaganizidwe ka Luntha Ka Dziko:

Uku ndi kukhala ndi chidziwitso chozama. Kaganizidwe ka luntha ka dziko sikanakhazikitsidwe pa Khristu:

Penyani kuti pasakhale wina wakulanda inu ngati cuma, mwa kukonda nzeru kwace, ndi cinyengo copanda pace, potsata mwambo wa anthu, potsata zoyamba za dziko lapansi, osati potsata Kristu; (Akolose 2:8).

Nzeru Za Dziko:

Nzeru ya dziko lapansi si nzeru ya Mulungu:

Pakuti nzeru ya dziko ina lapansi iri yopusa kwa Mulungu, Pakuti, kwalembedwa, iye agwira mzeru m'cenjerero lao; (1 Akorinto 3:19).

Njira Ya Dziko:

Njira ya dziko momwe dziko likuyendera ndi kugwirira ntchito:

zimene munayendamo kale, monga mwa mayendedwe a dziko lapansi lino, monga mwa mkulu wa ulamuliro wa mlengalenga, wa mzimu wakucita tsopano mwa ana a kusamvera; (Aefeso 2:2).

Mau A Dziko:

Mau a dziko ndi osemphana ndi Liu la Mulungu:

Iripo, kaya, mitundu yambiri yotere ya mau pa dziko lapansi, ndipo palibe kanthu kasowa mau. (1 Akorinto 14:10).

Mtendere Wa Dziko

Mtendere wa dziko ndi wa kanthawi, wosakhazikika ndipo nthawi zina wonyenga:

Mtendere ndikusiyirani inu, mtendere wanga ndikupatsani; Ine sindikupatsani inu monga dziko lapansi lipatsa. 5 Mtima wanu usabvutike, kapena usacite mantha. (Yohane 14:27).

Chisoni Cha Dziko

Chisoni cha Umulungu ndi chosiyana ndi cha dziko:

Pakuti cisoni ca kwa Mulungu citebenezira mtima kueipulumutso, cosamvetsanso cisoni; koma cisonicadziko lapansi cicita imfa. (2 Akorinto 7:10).

Maonedwe A Zinthu a Dziko

Dziko limadana ndi Mulungu:

Akazi acigololo inu, kodi simudziwa kuti ubwenzi wa dziko lapansi uti udani ndi Mulungu? Poto, iye amene afuna kukhala bwenzi la dziko lapansi adziika mdani wa Mulungu. (Yakobo 4:4).

Dziko limadana ndi okhulupirira:

Ngati dziko lapansi lida inu, mudziwa kuti lidada Ine lisanayambe kuda inu. Mukadakhala a dziko lapansi, dziko lapansi likadakonda zace za lokha; koma popeza simuli a dziko lapansi, koma Ine ndinakusankhani inu mwa dziko lapansi, cifukwa ca ici likudani inu. (Yohane 15:18-19).

Popeza kuti dziko ladzadzidwa ndi anthu ongotsata zofuna za thupi omwe amadana ndi okhulupirira, tikuyenera kuphunizira zambiri za mdani uyu wotchedwa “thupi.”

CHIGAWO CHACHIWIRI: THUPI

Dziko ndi mphamvu yoipa ya Satana yomwe amaigwiritsa ntchito kulimbana ndi okhulupirira kuchokera kunja kwa moyo wawo. Ndi kachitidwe ka zinthu ka anthu okonda za thupi. Thupi ndi mphamvu yomwe yoipa yomwe imalimbana ndi wokhulupirira koma kuchokera mkati mwake. Mzimu uja “wa thupi” womwe umagwira ntchito mdziko udzakhala ukugwira ntchito m’ moyo wanu ngati mungaupatse mpata. Mau oti “thupi” atha kutanthauza mnogu weni-weni wa munthu kapena nyama. Koma ili sithupi lomwe tikhale tikukambirana mu phunziro lino.

Baibulo limagwiritsanso ntchito mau oti “thupi” kutanthauza chikhalidwe chauchimo chachibadwidwe cha munthu. Thupi ndiye tsinde la kugalukira ndi mwano wonse pamaso pa Mulungu:

Pakuti ndiyesa kuti masauko a nyengo yatsopano sayenera kulinganizidwa ndi ulemerero umene udzaonetsedwa kwa ife. Pakuti ciyembekezetso ca colengedwa cilimilia bvumbulutso la ana a Molungu. Pakuti colengedwaco cagonietsedwa kuutsiru, cosafuna mwini, koma cifukwa ca iye amene anacigonjetsa, (Aroma 8:18-20).

Thupi ndi mphamvu yokakamiza ya mkati yomwe imadzionetsera yokha nkugalukira kudzera mu tchimo. Ili ndiye tanthauzo la thupi lomwe tigwiritse ntchito mu phunziro lino. Mau oti “nzeru za umunthu” kapena “munthu wakale” amagwiritsidwanso ntchito kufotokozera za chikhalidwe cha thupi cha munthu. Anthu onse ali ndi chikhalidwe choterechi:

Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa ucimo; coteru imfa inafikira anthu onse, cifukwa kuti onse anacimwa. (Aroma 5:12).

pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu;(Aroma 3:23).

CHILAKOLAKO CHA THUPI

Koma ndinena, Muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse chilakolako ca thupi. (Agalatiya 5:16)

Kodi chilakolako cha thupi ndi chiyani? Poyamba tiyeni tipeze tanthauzo la mau oti “chilakolako.” Chilakolako ndi chikhumbo-khumbo cha mphamvu, zofuna moyo, chikhalidwe cha munthu choyadzamira ku zoipa:

Koma zinthu izi zinacitika, zikhale zoticenjeza ife, kuti tisalakalake zoipa ife, monganso iwowo analakalaka. (1 Akorinto 10:6).

Kukhumba zoipa zomwe zikondweretse thupi lanu ndiye “chilakolako cha thupi.” Ndi chilakolako cha thupi, Satana amathira nkondo okhulupirira kuchokera mkati mwao. Ziri ngati nkondo ya pachiwani-weni mdziko. Mzimu ndi thupi lanu kumenyana wina ndi mnzake.

MABADWIDWE A CHILAKOLAKO:

Chilakolako kapena kukhumba zoipa, kumalowa mwa munthu kudzera zomvaimva za chilengedwe za munthu. Maso aona chinthu choipa kapena khutu kumva zinthu zauchimo. Kugwira, kulawa kapena kununkhiza kumene kutha kuyambitsa chilakolako. Umu ndi momwe Satana amagwiritsira ntchito zinthu zotizungulira kuti ayese thupi lathu. Maso, makutu, zogwira-gwira, kulawa kapena kununkhiza zimadzutsa maganizo kapena chikhumbokhumbo choipa mwa ife. Ichi ndiye chilakolako ndipo ndi zomwe zimakuyesani inu kuti muchite choipa.

Pozindikira kuti ciyesedwe ca cikhulupiriro canu cicita cipiriro. Koma cipiriro cikhale nayo nchito yace yangwiro, kuti mukakhale angwiro ndi opanda cirema, osasowa kanthu konse. Koma wina wa inu ikamsowa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza; ndipo adzampatsa iye, Koma apemphe ndi cikhulupiriro, wosakayika konse; pakuti wokayikayo afanana ndi pfunde la nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuwinduka nayo. Pakuti asayese munthu uyu kuti adzalandira kanthu kwa Ambuye; munthu wa mitima iwiri akhala wosinkhasinkha pa njira zace zonse. Wodala munthu wakupirira poyesedwa; pakuti pamene wabvomerezeka, adzalandira korona wa moyo, amene Ambuye adalonjezera iwo akumkonda iye. Munthu poyesedwa, asanena, Ndiyisedwa ndi Mulungu; pakuti Mulungu sakhoza kuyesedwa ndi zoipa, ndipo iye mwini sayesa munthu: koma munthu ali yense ayasedwa pamene cilakolako cace ca iye mwini cimkokera, nicimnyenga. (Yakobo 1:3-14).

Kumbukirani, Mulungu sayesa munthu. Mumayesedwa pamene mwakokedwa ndi zikhumbokhumbo zoipa zathupi. Koma simukuyenera kugonjera ku zimenezi. Mulungu nthawi zonse amapereka njira yopulumikirapo:

Sicinakugwerani inu ciyeso koma ca umunthu; koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza; koma pamodzi ndi ciyeso adzaikanso populumukirapo, kuti mudzakhoze kupirirako. (1 Akorinto 10:13)

Pakuti maganizo amagwiritsidwa kuyesa thupi, Paulo akuchenjeza:

Cifukwa cisamaliro ca thupi cidana ndi Mulungu; pakuti sicigonja ku cilamulo ca Mulungu, pakuti sicikhoza kutero. Ndipo iwo amene ali m'thupi sangathe kukondweretsa Mulungu. (Aroma 8:7-8).

Muphunzira momwe maganizo amakhallira bwalo la nkondo yauzimu.

ZOTSATIRA ZA CHILAKOLAKO

Mukagonjera ku zilakolako, yesero limafika ndipo mukagonjera yeserolo, limakutsogolerani ku uchimo womwe umafikitsa ku imfa:

Pamenepo cilakolakoco citaima, cibala ucimo; ndipo ucimo, utakula msinkhu, ubala imfa. (Yakobo 1:15).

Dziko laonongeka chifukwa cha chilakolako:

mwa izi adatipatsa malonjezano a mtengo wace ndi akuru ndithu; kuti mwa izi mukakhale oyanjana nao umulungu wace, mutapulumuka ku cibvundi ciri pa dziko lapansi m'cilakolako. (2 Petro 1:4).

Thupi lanu laonongeka chifukwa cha chilakolako:

kuti mubvule, kunena za makhalidwe anu oyamba, munthu wakale, wobvunda potsata zilakolako za cinyengo; (Aefeso 4:22).

UBALE WA MZIMU KU THUPI

(Agalatiya 5:17). Mukapulumsidwa ndi kudzadzidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera, Mzimuyo amakhala mwa inu. Mzimu Woyera mu mzimu mwanu amatsutsa zilakolako za thupi. Thupi lanu limalimbana ndi mzimu wanu komanso Mzimu wa Mulungu mwa inu. Thupi limakukopani kuti muchite zinthu zoipa. Ichi ndi chifukwa chake simukhala moyo wosangalatsa Mulungu m'mene m'mafunira.

Paulo anafotokozera za nkondo iyi ya pakati pa thupi ndi mzimu mu Aroma 7:

Aroma 7:21-23 Ndipo coteru odipeza lamulo ili, kuti, pamene ndifuna cabwino, coipa ciriko. Pakuti monga mwa munthu wa m'kati mwanga, ine ndikondwera ndi cilamulo ca Mulungu: koma ndiona lamulo lina m'ziwalo zanga, lirikulimbana ndi lamulo la mtima wanga, ndi kundigonjetsa kapolo wa lamulo la m'ziwalo zanga. (Aroma 7:21-23).

NTCHITO ZA THUPI

Zilakolako za thupi, ngati sizigonjetsedwa, zimatsogolera ku ntchito za uchimo za thupi zomwe zimakufikitsani ku imfa ya muuzimu:

Ndipo nchito za thupi zionekera, ndizo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; zimene ndikucenjezeni nazo, monga ndacita, kuti iwo akucitacita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu. (Agalatiya 5:19-21).

Mndandanda wa machimowu utha kuikidwa m'magawo anayi a machimo:

- Machimo opembedza: Kupembedza mafano, ndi ufiti
- Machimo a chiwerewere: Chigololo, chiwerewere, chidetso, ndi chisiliro chonyansa.
- Machimo a munthu payekha: Kuledzera ndi mchezo
- Machimo a ubale: chidano, variance, kaduka, mkwiyo, ndeu, kunyoza, nsanje ndi kupha.

Tchimo liri lonse mwa machimo awa afotokozeredwa mwa tsatane tsatane mu phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa “Utumiki wa Mzimu Woyera.” Aunikiridwa mowasiyanitsa ndi chipatso cha Mzimu Woyera chomwe chikuyenera kuchichengetera mkati mwathu.

MPHAMVU ZAKUMDIMA ZOPOSA

Dziko ndi thupi zimaphatikizana ndi Satana pamodzi ndi ziwanda zake kumenyana ndi okhulupirira. Izi ndi mphamvu zauzimu za kumdima. Mu phunziro linali muphunzira za njira zomenyera nkondo yauzimu polimbana ndi mphamvu zauzimu za kumdima.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Mavesi Otsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Kodi tanthauzo la mau oti “thupi” ndi lotani molingana ndi phunziro lino?

3. Kodi tanthauzo la mau oti “dziko” ndi lotani molingana ndi phunziro lino?

4. Kodi mfumu ya dziko lapansi ndi ndani?

5. Lembani mwachidule machitidwe a dongosolo la dziko lapansi.

6. Kodi tsinde la momwe zinthu zirili lero mdziko ndi chiyani?

7. Kodi dziko limaona okhulupirira motani?

8. Kodi tanthauzo la “chilako-lako cha thupi” ndi lotani?

9. Kodi chilakolako chimabadwa bwanji?

10. Chimachitika ndi chiyani ngati munthu satha kudziletsa pa zilakolako za thupi?

11. Perekani mavesi omwe amakamba za ntchito zathupi.

(Mayankho a mafunsowa ali ku mapeto kwa bukhu lino).

MACHITA-CHITA A LUSO

1. Werengani zambiri za ntchito zathupi mu Agalatiya 5:19-21.
2. Siyanitsani ntchito zathupi zoipazi ndi chipatso cha Mzimu mu Agalatiya 6:22-23.
3. Werengani Yohane 1:1-15 ndi chaputala 3. Onani chikondi chachikulu cha Mulungu ku dziko posatengera uchimo womwe watenga malo. Kodi Mulungu anachita chiyani poonetsa chikondi chake? Kodi dziko linachita chiyani ku chikondichi?
4. Werengani zambiri za mayesero.
 - Satana amatchedwa woyesa: Matthew 4:3; 1 Atesalonika 3:15
 - Mulungu sayesa anthu kuchita zoipa: Yakobo 1:13-14
 - Munthu amayesedwa ndi:
 - a. Anthu: Mateyu 16:1; 19:3; 22:35; Marko 8:11; 10:2; Luka 11:16; Yohane 8:6
 - b. Satana: Mateyu 4:1; Marko 1:13; Luka 4:2; 1 Akorinto 7:5
 - c. Zilakolako zanu: Yakobo 1:13-14
 - d. Chuma: 1 Timoteo 6:9
 - Mukuyenera kupemphero kuti musalowe m'mayesero: Mateyu 26:41; Luka 11:4; Marko 14:38; 22:46
 - Yesu anayesedwa, koma sanachimwe: Ahebri 2:18; 4:15
 - Ndinu wodala ngati mupirira mayesero: Yakobo 1:12
 - Mulungu atha kukupulumutsani ku mayesero: Ahebri 4:15; 2 Petro 2:9; 1 Akorinto 10:13
 - Mayesero amabweretsa amapsinja koma muchiyese chimwemwe chokha choka: Yakobo 1:2; 1 Petro 1:6.
5. Kodi mukuzunzika ndi chilakolako chomwe chakuika mu yesero mpakana kuchimwa? Tsatani njira yomenyera nkhondo ya pa 1 Yohane 1:8-9.
6. Pamene Paulo amakamba za kulimbana mkati mwake amanthauza kulimbana kwa pakati pa thupi ndi mzimu. Onani Agalatiya 5:16-26.

CHAPUTALA 8

MACHENJELERO A SATANA

ZOLINGA

Mukamaliza chaputala mukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kulemba mwachidule machenjerero a mdani pa Mulungu
- Kulemba mwachidule machenjerero a mdani pa maiko
- Kulemba mwachidule machenjerero a mdani pa osakhulupirira
- Kulemba mwachidule machenjerero a mdani pa okhulupirira

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire: ameneyo mumkanize okhazikika m'cikhulupiriro, podziwa kuti zowawa zomwezo zirimkukwaniridwa pa abale anu ali m'dziko. (1 Petro 5:8-9)

MAU OYAMBA

Phunziro lino limaonetsera machenjerero a mdani, Satana modumphadumpha. M'phunziro linalo, muona za “Dongosolo la Nkhondo” la Mulungu. Kenako, mutatha kulandira zida za nkhondo yauzimu, muphunzira tsatane-tsatane wa dongosolo longonjetsera machenjerero onse a mdani. Koma poyamba, mukuyenera kumvetsa za machenjerero ake pa Mulungu, maiko, osakhulupirira, ndi okhulupirira.

M'DANI NDI MULUNGU

Tchimo loyamba la Satana ndilo kufuna kufanana ndi Mulungu, ndiye mphamvu ndi machitachita ake onse zimalunjika kwenikweni kwa Mulungu. Zina zonse zomwe amachita komanso chikhalidwe chake zimaoneka kuti zikuchokera pa khumbo lake loukira Mulungu.

Mwachitsanzo, zomwe Satana anachita pa Adam ndi Hava, kunali kulimbana kweni kweni kwa chikhalidwe cha Mulungu ndi mphamvu zake (Genesisi 3:1-5). Satana anapangitsa Kaini kupha Abele potsutsana ndi Mulungu (1 Yohane 3:10-12). Mutha kuwerenga nkhondo zonse za Satana ndipo muona kuti zimalunjika pa Mulungu, chikhalidwe chake, ndi ntchito zake.

Satana amakhala akutsutsana ndi Mulungu mu zochita zake ndi chikhalidwe chake.

Mwachitsanzo, Mulungu ndi chikondi pamene Satana ndi wankhaza ndipo amalimbikitsa nkhanza (1 Yohane 3:7-15). Mulungu ndi moyo ndipo amalenga moyo pamene Satana amalimbikitsa imfa ndi chionongeko (Ahebri 2:14).

Satana samangolimbana ndi Mulungu ndi chikhalidwe chake chokha, amalimbananso ndi dongosolo lake. Amakana kuti Mulungu alipo (Masalimo 14:1-3). Amalimbikitsa mabodza

(Aefeso 2:2; 2 Atesalonika 2:8:11); ndipo ndiye amene ali kumbuyo kwa zipembedzo zonama, za maula ndi ziphunzitso zonyenga. Zipembedzo zoipa za Satana zimabweretsa aphunzitsi onyenga, aneneri onyenga, ndi akhristu onyenga. Muphunzira zambiri za izi mu phunziro lotchedwa “Zoipa Zauzimu M’zakumwamba.”

Satana adzafika pachimake kugalukira Mulungu ndi dongosolo lake mu nthawi ya “Nkhondo Yotsiriza” yomwe ili m’phunziro lomaliza la buku lino. Posatengera machenjerero ake onsewa, Satana ndi mphamvu zonse za kumdima sichipsezo konse kwa Mulungu wathu wamphamvu.

M’DANI NDI MAIKO

Satana amatchedwa “mulungu wa dziko lapansi” ndipo amaphatikizapo anthu osakhulupirira komanso angelo a ziwanda (2 Akorinto 4:4) Iye analonjeza kupereka maiko kwa Yesu nthawi ya kuyesedwa kwake ndipo Yesu sanatsutse za umwini pa maiko. Yesu anangokana kuukira Mulungu mu njira yogonjera Satana ngati njira yopezera ulamuliro (Mateyu 4:8-10).

Satana amagwiritsa ntchito ziwanda kusocheretsa maiko, kutsogolera anthu ndi atsogoleri awo kuchoka pamaso pamaso pa Mulungu. Nchifukwa chake tikuona atsogoleri ndi maulamuliro ambiri ankhaza m’maiko ambiri. Ndi zomwe zimapangatsa kusemphana maganizo ndi nkhondo pakati pa maiko. Satana amalimbana kwambiri mpingo pamodzi ndi anthu ake osankhika, Israel. Amagwiritsanso ntchito maboma kutsekereza kufalikira kwa Uthenga Wabwino.

Mu nthawi ya chizunzo chachikulu, Satana adzalamulira zochitika za m’maiko khumi kudzera mwa Wokana Khristu. Kubweranso kwa Yesu kukachitika, Satana adzamangidwa kwa zaka chikwi (Chibvumbulutso 20:3). Akamasulidwa, adzakopa maiko komaliza kuti asonkhane ndi kulimbana ndi Mulungu komanso Yerusalemu (Chibvumbulutso 20:7-10). Kenako, maufumu onse a dziko lapansi komanso Ufumu wa Satana udzakhala zidzakhala mu Ufumu wa Ambuye wathu Yesu Khristu.

Satana ali ndi njira yamphamvu yothana ndi anthu osakhulupirira. Amaphimba maganizo a anthu kuti asakhulupirire Uthenga Wabwino. (2 Akorinto 4:3-4) ndipo amakwatula choonadi cha Uthenga pamene iwo aumva ndi cholinga choti asakhulupirire (Luka 8:12). Chifukwa cha ichi, Uthenga Wabwino umaoneka wopusa ndi wosafunikira kwa iwo omwe ali mu uchimo (1 Akorinto 1:18).

Satana amakolanso osakhulupirira ambiri kulowa mu zipembedzo zonyenga (1 Timoteyo 4:1-3) ndipo amawatsogolera kuyenda molingana ndi “dongosolo la dziko lapansi” lomwe ndi maganizidwe a chikunja a masiku ano. Ngakhale maganizidwewa amakhala osiyanasiyana potengera m’badwo komanso chikhalidwe komabe amakhala okomera anthu osati Mulungu. Nthawi ndi nthawi Satana amakhala akubzala mbeu ya kuukira (uchimo) m’mitima ndi m’maganizo a anthu osakhulupirira.

Mwa zina Mzimu Woyera amagwira ntchito yolimbana ndi Satana kuti aombotse miyoyo ya osakhulupirira. Iye amapanga amuna ndi akazi kumva kutsutsika pa kuukira Mulungu kwao (Yohane 16:7-11).

MDANI NDI OKHULUPIRIRA

Munthu akalandira Yesu ngati Mpulumutsi, sizitanthauza kuti basi nkondo yatha, ayi. Apapa mwangopambana kulimbana koyamba chabe, nkondo yeni yangoyamba.

Muphunzira zambiri mwatsata-tsatane za machenjerero a Satana pamene mukupitiriza kuphunzira ndi kupatsidwa zipangizo zipangizo zauzimu ndi kukusidwa kukalimbana ndi mdani. Koma nkondoyi itha kuikidwa m'magulu anayi. M'moyo wa wokhulupirira Satana amalimbana ndi zinthu izi:

MAU A MULUNGU

Satana akupangitsani kukayikira Mau a Mulungu, kuonjezera, kuchotsera kapenanso kuwasokoneza. Kumbukirani kuti izi ndi zomwe zinachitika pakuyesedwa kwa Hava. Nchifukwa chake kusanthula Mau a Mulungu kuli kofunika kuti musasokoretse ndi machenjerero a Satana.

KUPEMBEDZA MULUNGU

Kuukira kwa Satana koyamba nkoti ankafuna kupembedzedwa, ndiye amalimbana ndi kupembedza kwa okhulupirira. Adzayesetsa kukutchingani kuti musapembedze Mulungu ndi kukutsogolerani ku kupembedza kwachinyengo kapena kwa kuthupi.

UBALE WANU NDI MULUNGU

Satana amalimbana ndi ubale wanu ndi Mulungu. Amakunenezani ndi kukunamizirani, kukuyesani kuti musate ntchito za kuthupi, mutengeke ndi zochitika za dziko lapansi, ndi kuti muzidalira nzeru ndi kuthekera kwanu kokha. Ngati Satana angakwanitse kusokoneza ubale wanu ndi Mulungu, ndiye kuti savutika kuthana ndi gawo lina la moyo wanu...

KUTUMIKIRA MULUNGU

Satana amalimbananso ndi ntchito yanu yotumikira Mulungu. Ayesetsa kukutchingani kuti musakwaniritse ntchito yomwe Mulungu anakuitanirani kudzera m'chizunzo, ngozi za dzidzidzi, kufooketsedwa, kusapemphera, ndi kutanganidwa ndi zosamalira za moyo uno. Satana amalimbananso ndi ntchito ya Mulungu kudzera m'kubweretsa aphunzitsi onyenga mu mpingo (2 Akorinto 11:13-15; 2 Petro 2:1-19; Mateyu 13:38-39).

Pamene Mulungu akufesa mbeu zabwino mu utumiki wanu, Satana amafesa namsongole amene ndi "ana a woipayo." Amalimbikitsa magawano mu thupi la Khristu poyesera kuononga ntchito ya Mulungu ndi zolinga zake m'moyo ndi mu utumiki wanu.

NDIYE MUNGATANI?

Machenjerero a Satana ndi osiyana-siyana komanso amphamvu pamene akulimbana ndi ntchito za Mulungu, maiko, osakhulupirira ndi okhulupirira.

Titatha kuphunzira za mdani, mphamvu za kumdima, dera la mdani ndi machenjerero ake m'machaputala anayi apitawa mutha kuyamba kukhala ndi mantha. Komano muona mu chaputala chikubwerachi kuti Mulungu ali ndi dongosolo lomenyera nkondo lamphamvu kwambiri kuposa machenjerero onse a mdaniyo.

Tsopano muli okonzeka kuphunzira za dongosolo la Mulunguli ndi kupatsidwa mphamvu zauzimu ndi kukusidwa kukamenya nkondo.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Lembani mwachidule machenjerero a Satana polimbana ndi Mulungu.

3. Lembani mwachidule machenjerero a Satana polimbana ndi maiko.

4. Lembani mwachidule machenjerero a Satana polimbana ndi osakhulupirira.

5. Lembani mwachidule machenjerero a Satana polimbana ndi okhulupirira.

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto a bukhu lino).

MACHITA-CHITA A LUSO

1. Fufuzani dziko lomwe mukukhala. Kodi ndi njira ziti za Satana zomwe zikugwira ntchito?
2. Fufuzani za anthu osakhulupirira m'dera lanu maka awo amene mumawapemphelera nthawi ndi nthawi. Kodi mdani sanawamange m'maso kuti asaone mphamvu ya Uthenga Wabwino. Kodi akukwatula Uthenga Wabwino ukangoperekedwa kwa iwo? Kodi anthu akulowetsedwa m'zipembedzo zonyenga? Kodi akukhala monga mwa dziko lapansi? Tengati zimenezi zikhale zopembedzera zanu.
3. Taonani magawo anayi awa omwe Satana amatsutsa:
 - Amatsutsa Mulungu pamaso pa okhulupirira: Genesis 3:1-5
 - Amatsutsa okhulupirira pamaso pa Mulungu: Yobu 1-2; Chibvumbulutso 12:9-10
 - Amatsutsa okhulupirira pamaso pa chikumbumtima chake chomwe: Yeremiya 31:34; Aroma 8:33-39.
 - Amatsutsa okhulupirira kudzera mwa okhulupirira ena: Mateyu 16:13-23; Aroma 8:33-39.
4. Talingalirani za moyo wanu. Pa mpata uli m'musiwu, lembani momwe Satana amalimbirana ndi inu m'madera a Mau a Mulungu, kupembedza kwanu, ubale wanu ndi Mulungu komanso utumuki wanu kwa Mulungu:

Mau a Mulungu:

Kupembedza Mulungu:

Ubale wanu ndi Mulungu:

Ntchito yanu yotumikira Mulungu:

M'maphunziro otsatirawa muphunzira njira zomwe mungagwiritse ntchito polimbana ndi woipayo m'dera liri lonse la madera omwe tatchulawa.

CHAPUTALA 9

DONGOSOLO LA MULUNGU LOMENYERA NKHONDO

ZOLINGA

Mukamaliza chaputala chino mukuyenera kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo
- Kuzindikira cholinga cha Mulungu
- Kuzindikira cholinga chomwe Yesu anabwelera ku dziko lapansi
- Kufotokozerera dongosolo la Mulungu lomenyera nkhondo lokhala ndi mitu isanu ndi umodzi.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Mphepo iomba pomwe ifuna, ndipo ukumva mau ace, komavsudziwa, kumene icokera, ndi kumene imuka; coteru ali yense wobadwa mwa Mzimu. (1 Yohane 3:8).

MAU OYAMBA

Chaputala chino chikutipatsira dongosolo lomenyera nkhondo yauzimu. Dongosololi lagonera pakumvetsa cholinga cha nkhondo yauzimu komanso lagonera pakulumikizana ndi Wamkulu wa Nkhondo wathu kudzera m'pemphero, kusala kudya, ndi mau olembedwa a Mulungu.

Ngati simumvetsa cholinga ndi dongosolo la Mulungu, mutha kuyesedwa kugwa mphwayi chifukwa cha zovuta za moyo uno. Ichi ndi chifukwa chake asilikari ambiri a Khristu amalephera kuchita bwino pakumenya nkhondo: Satha kumvetsa cholinga chazimu chomwe chili mu nkhondo zawo.

Ndipo tsopano ndinena ndi inu, Lekani anthu amenewa, nimuwalole akhale; pakuti ngati uphungu umene kapena nchito iyi icokera kwa anthu, idzapasuka; koma ngati icokera kwa Mulungu simungathe kuwapasula; kuti kapena mungapezeke otsutsana ndi Mulungu. (Machitidwe 5:38-39)

CHOLINGA CHA NKHONDO

Kuyambira kale, nkhondo iliyonse yomwe yamenyedwa pa dziko lapansi imakhala ndi cholinga. Tisanaone dongosolo la nkhondo la Mulungu, ndi zofunika kwambiri kumvetsa cholinga cha nkhondo yauzimu. Izi zikuphatikizapo zolinga za Mulungu Atate ndi Yesu Khristu Mwana.

ZOLINGA ZA MULUNGU

Ndi cholinga cha Mulungu kuti:

kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:10).

Kuchokera pachiyambi, Satana wakhala akulimbana ndi kukwaniritsidwa kwa cholinga ichi. Nkhondo yanu ya muuzimu ndi yolumikizika ku cholinga ichi cha Mulungu. Satana amayesetsa kupangitsa mtima wanu, mzimu ndi maganizo anu kuti zizilemekeza iye osati Yesu Khristu.

Mulungu amagwira ntchi mwa inu kuti akwaniritse zolinga zake:

pakuti wakucita mwa inu kufuna ndi kucita komwe, cifukwa ca kukoma mtima kwace, ndiye Mulungu, (Afilipi 2:13).

Mulungu amagwiranso ntchito m'moyo wanu kuti akwaniritse zolinga zake:

Ndipo musapereke ziwalo zanu kuucimo, zikhale zida za cosalungama; koma mudzipereke inu nokha kwa Mulungu, monga amoyo ataturuka mwa akufa, ndi ziwalo zanu kwa Mulungu zikhale zida za cilungamo, (Aroma 6:13).

Mukadzipereka nokha kuti mukhale “chipangizo cha chilungamo kwa Mulungu,” zimatanthauza kuti mwabweretsa moyo ndi utumiki wanu chindunji ndi zolinga ndi dongosolo la Mulungu. Mukatero, Satana, mdani wa Mulungu, amayamba kukusakasakani.

ZOLINGA ZA YESU

Yesu anati:

Iye wocita cimo ali wocokera mwa mdierekezi, cifukwa mdierekezi amacimwa kuyambira paciyambi. Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge ntchito za mdierekezi, (1 Yohane 3:8).

Cholinga chomwe anabwelera pa dziko lapansi ndicho kuti akaononge ntchito za Satana. Izi zinamuika pa mulingo wotsutsana ndi mdaniyo:

Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10).

Kuchokera pa chiyambi cha utumiki wake padziko lapansi, Yesu anakhala akuononga ntchito za Satana:

- Anabvumbulutsa ukapolo wa tchimo (Yohane 8:34).
- Anakhululukira machimo (Mateyu 9:1-8; Marko 2:1-12,17; Luka 4:17-32).
- Anatsindika za kufunika kwa chiyero cha mu mtima osati maoneke chabe a kunjja (Mateyu 15:16-20; Maro 7:20-23; Luka 6:45; 11:39).
- Anachiritsa odwala (Mateyu 11:5).
- Anaukitsa anthu kwa akufa (Marko 5:35-43; Luka 8:49- 56; Yohane 11).
- Anamasula anthu ku mphamvu ya ziwanda (Mateyu 8:16)

Mwachidule, anaononga ntchito za Satana m'mitima, miyoyo, maganizo ndi matupi a anthu:

Akhungu alandira kuona kwao, Ndi opunduka miyendo ayenda, akhate akonzedwa, indi ogontha akumva, ndi akufa aukitsidwa, ndi kwa aumphawi ulalidwa uthenga wabwino. (Mateyu 11:5).

Yesu sanangoononga ntchito za Satana, anabweretsanso machenjerero ake onse poyera:

- Anaphunzitsa za chinyengo cha Satana chomwe chidzakule kwambiri m’masiku otsiriza padziko lapansi Mateyu 24-25; Marko 13; Luko 17:22-37; 21:8-36; Mateyu 24-25).
- Anachenjeza za Satana yemwe anali ndi kuthekera koononga moyo (Mateyu 10:28).
- Analankhula za kufunika komanga munthu wamphamvuyo tisanaononge katundu wake (Mateyu 12:26-30; Marko 3:23-27; Luka 11:17-24).
- Anabvumbulutsa momwe Satana amayesera kutchingira Mau a Mulungu kuti asakhale amphamvu m’mitima mwa anthu (Mateyu 13:38; Marko 4:15; Luka 8:12).
- Anaulula iwo amene sanali olungama pamaso pa Mulungu kuti ali a “tate wao, mdierekezi” (Yohane 8:44-47).
- Anabvumbulutsa kuti Satana ali mfumu ya dziko lapansi (Yohane 14:30).

KUGAWIKANA KWAKUKURU

Ngakhale Yesu anabwera ndi mtendere (Yohane 14:27), komanso mtendere ndi Mulungu (Aroma 5:1), Iye anabweretsanso kugawikana:

Musalinalire kuti nelidadzera kuponya mtendere pa dziko lapansi; sinelinadzera kuponya mtendere, koma lupanga. 3 Pakuti ndinadza kusiyanita munthu ndi atate wace, ndi mwana wamkazi ndi amace, ndi mkazi wokwatiwa ndi mpongozi wace: ndipo 4 apabanja ace a munthu adzakhala adani ace. (Mateyu 10:34-36).

Yesu anagawa anthu onse m’magulu awiri. Nzosatheka kukhala chikati-kati:

Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa ambuye awiri: pakuti pena adzamuda mmodziyo, ndi kukonda winayo; pena adzakangamira kwa mmodzi, nadzanyoza wina. Simungathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi wa Cuma. (Mateyu 6:24).

(Iye amene sali ndi ine, atsutsana nane... (Luka 11:23).

Yesu analankhula za kugawikana uku mu nkhani yake ya njira ziwiri, yopapatiza ndi yotakata. Anachenjeza za chinyengo cha Satana kukopa anthu kunka ku njira yotakata yomwe anthu ambiri analimo (Mateyu 7:13-14). Kudzera mu nkhani ya munthu wolembera ndi Lazaro wosauka (Luka 16:19-31), Yesu anachotsa chotchija cha pakati pa moyo ndi imfa. Anawalola kuti adziononere okha zotsatira zosankha njira ya chitaiko.

Chifukwa choti anaononga ndi kubvumbulutsa ntchito za Satana, moyo wa Yesu unali pa chiopsezo nthawi yonse ya utumiki wake panso pano. Mdaniyo anayesetsa kumuononga kapena kumuletsa kuti asakwaniritse cholinga cha Mulungu chomwe anabwelera. Atangobadwa, chiwembu choti aphedwe chinachitika. Mu utumiki wake wonse Satana anali akuyesa-yesa

kuthana ndi moyo wa Yesu ndipo ulendo wina chiwembu china chinalephereka. Anatsutsana ndi mphamvu ya ziwanda, atsogoleri a chipembedzo, otsatira ake komanso Satana.

Mukaika moyo wanu chindunji ndi madongosolo ndi zolinga za Yesu pakumalindira ngati Mpulumutsi, umakhala mbali imodzi ya gulu la asilikari lolimbana ndi Satana. Zolinga za Yesu zimakhala zolinga zako ndipo izi zimakuikani kukhala mdani wa Satana.

DONGOSOLO LA NKHONDO

Pali njira zosiyana-siyana za m’Baibulo zomwe zingagwiritsidwe ntchito pomenya nkhondo yauzimu, komano njira yabwino kwa okhulupirira ipezeka pamene tiona zomwe Yesu anachita pothana ndi mdani. Nkhondoyi yagonera kwambiri pa mfundo zisanu ndi imodzi:

- Mau a Mulungu
- Mphamvu ndi ulamuliro zochita kupatsidwa
- Pemphero
- Kusala kudya
- Mfungulo za mu Ufumu
- Dzina la Yesu

MAU A MULUNGU

Kukumana kwa Yesu ndi Satana maso ndi maso kunachitika pa nthawi ya kuyesedwa kwake ndi mdaniyo. Ndipo kukumanaku kunabvumbulutsa gawo limodzi lofunika kwambiri la dongosolo lathu lauzimu lomenyera nkhondo. Tisanapitilire ndi phunziro, werengani za momwe Satana anamayesera Yesu mu Mateyu 4:1-11; Marko 1:12-13, ndi Luka 4:1-13.

Poyamba Satana anayesera kumpanga Yesu kuti asandutse miyala kuti ikhale mkate. Mphamvu ya Yesu yomwe posachedwapa igwiritsidwe ntchito kusandutsa madzi kukhala vinyo ikanagwiritsidwa ntchito kusandutsa miyala kukhala mkate. Yesu akanachita izi akanakhala kuti akugwiritsa ntchito mphamvu mosadalira Mulungu komanso pa zofuna zake.

Kenako, anamutengera pamwamba pa kachisi kuti azigwetse pansi. Zindikirani kuti anamuuza Yesu kuti, “Uzigwetse pansi.” Satana sakanatha kumugwetsa Yesu chifukwa mphamvu zake nzoperewera. Satana amangokwanitsa kukukopani kuti muchimwe, koma sangakugwetseni. Monga mwaphunzira kale, munthu aliyense amayesedwa pamene wakokeredwa ku zilakolako zake zomwe. Munthu sakakamizidwa kuchimwa koma kukopedwa kuti achimwe. Mu yesero ili, Satana akugwiritsa ntchito Mau a Mulungu kuti achitire umboni zomwe amalankhulazo, koma anawagwiritsa ntchito mauwo molakwika (Mateyu 4:6). Kugwiritsa ntchito Mau a Mulungu ndi chenjerero lalikulu la Satana.

M’mayesero ake onse awiri, Satana amayamba ndi mau oti, “NGATI uli Mwana wa Mulungu,” chita chakuti. Yesu akanatsatira zolankhula za Satana, zikanatanthauza kuti chitsimikizo cha Mulungu kuti Yesu ndi mwana wake chinali chosakwanira. Mulungu anali atalankhula kale kuchokera kumwamba kutsimikizira za ubale wake ndi Yesu (Mateyu 3:17). Satana amakonda

kulimbana kwambiri ndi ubale wathu ndi Mulungu. Yesero lomaliza la Satana linali kufuna kupembedzedwa. Iye analonjeza kumpatsa Yesu maufumu onse a dziko lapansi ngati malipiro ake.

M'mayesero atatu onsewa mutha kuona mphamvu zoipa za dziko, thupi ndi Satana zikulimbana ndi Yesu. Yesu anathana ndi mayesero onse a Satana pogwiritsa ntchito Mau a Mulungu. Baibulo ndi chida chazimu champhamvu kwambiri ndipo ndi gawo limodzi la zida za nkondo za Mulungu zomwe tiphunzire kutsogoloku. Limatchedwa “Lupanga la Mzimu.” Mau a Mulungu ndi bukhu louziridwa lokhalo la nkondo yauzimu. Mabuku ena amakhalanso ofunika koma ngati akugwirizana ndi Mau a Mulungu.

Pothana ndi mayesero a Satana, Yesu anagwiritsa ntchito Mau a Mulungu. Yesu anagwiritsa ntchito mavesi okhawa omwe amagwirizana ndi nkondo imene akumenya pa nthawi imeneyo. Samangolakatula mavesi kuyambira Genesisi mpaka Chibvumbulutso ayi. Yesu anati, “kwalembedwa...” Mukagwiritsa ntchito mavesi okhawa ogwirizana ndi nyengo yanu, muonetsetse kuti akugwirizana ndi zomwe Baibulo lonse likunena. Mavesiwo akuyenera agwiritsidwe ntchito molingana ndi nkhani yomwe ikukambidwa mu ndime imeneyo ndipo zigwirizane ndi chiphunzitso chonse cha Baibulo.

Kuti tigwiritse ntchito bwino mavesi mu nkondo yauzimu, mukuyenera tsono kudziwa Mau a Mulungu. Muwerenge, muwalingalire ndi kuloweza. Kugonjetsedwa kwambiri komwe takumana nako kwachitika chifukwa chosadziwa Mau a Mulungu:

Koma Yesu anayankha, nati kwa iwo, Mungolakwa a osadziwa malembo, kapena mphamvu za Mulungu. (Mateyu 22:29).

Mau a Mulungu ndi bukhu lathu la nkondo ndipo amabvumbulutsa dongosolo la nkondo la Mulungu.

ULAMULIRO NDI MPHAMVU ZOCHITA KUPATSIDWA

Gawo lachiwiri la dongosolo la nkondo la Mulungu lakhazikika pa ulamuliro ndi mphamvu pa Satana zomwe Yesu anapatsa ophunzira ake.

Koma unyinjira wa anthu, pamene anadziwa, anamtsata Iye; ndipo iye anawalandira, nalankhula nao za Ufumu wa Mulungu, naciritsa amene anasowa kuciritsidwa. (Luka 9:1).

Ulamuliro ndi mphamvu ndi zinthu ziwiri zosiyana. Titengere chitsanzo cha wapolisi. Ali ndi unifolomu ndi nyota ngati zizindikiro za ulamuliro wake. Ulamuliro wake ulipo chifukwa cha udindo womwe ali nawo m'boma. Ndiye chifukwa choti si yense amalemekeza ulamuliro womwe wapolisi ali nawo, iye amatenganso mufti. Mfutiyo ndiye mphamvu zake.

Ulamuliro wanu pa Satana umabwera kudzera mwa Yesu Khristu and chimene muli mwa Iye monga wokhulupirira. Koma mphamvu zanu zimabwera kudzera mwa Mzimu Woyera.

- Kudandaulira Ambuye Eksodo 32:11
- Kufunafuna Mulungu Yobu 8:5
- Kufunafuna nkhope ya Ambuye Masalimo 27:8
- Kupemphelera Yobu 8:5; Yereimiya 36:7

MOYO WA PEMPHERO WA YESU

Pemphero inali njira yodalirika kwa Ambuye Yesu:

Yesu anaika pemphero patsogolo:

- Amapemphera nthawi iliyonse masana kapena usiku: Luka 6:12-13
- Pemphero linali patsogolo osati kudya Yohane 4:31-32
- Pemphero linali patsogolo osati utumiki: Yohane 4:31-32

Pemphero limaperekeza chochitika chilichonse chofunika:

- Pamene amabatizidwa Luka 3:21-22
- Ulendo wake woyamba wa utumiki Marko 1:35; Luka 5:16
- Asanasankhe ophunzira Luka 6:12-13
- Asanadyetse komanso atamaliza kudiyetsa anthu zikwi zisanu: Mateyu 14:19, 23; Marko 6:41, 46; Yohane 6:11, 14-5
- Podyetsa anthu zikwi zinayi Mateyu 15:36; Marko 8:6, 7
- Petro anabvomereze Luka 9:18
- Yesu anasandulike pa phiri Luka 9:18, 29
- Pakubwerera kwa makumi asanu ndi awiriwo Mateyu 11:25; Luka 10:21
- Pa manda a Lazaro Yohane 11:41-42
- Pakudalitsa ana Mateyu 19:13
- Pakubwera kwa Aheleni ena Yohane 12:27-28
- Lisanafike ola la msautso wake Mateyu 26:26-27; Marko 14:22-23; Luka 22:17-19
- Kupemphelera Petro: Luka 22:32
- Kuti Mzimu Woyera aperekedwe: Yohane 14:1-6
- Pa njira ya ku Emmau: Luka 24:30-31
- Asanakwere kunka kumwamba: Luka 24:50-53
- Kupempherera omutsatira ake: Yohane 17
- Pemphero lomwe Yesu anaphunzitsa liri pa Mateyu 6:9-13.

MITUNDU YA PEMPHERO

Paulo akupempha ophunzira kuti apemphere nthawi zonse ndi “mapemphero onse” (Aefeso 6:18). Pena analemba kuti “kupemphera ndi mtundu uliwonse wa pemphero.” Izi zikutanthauza kuti pali milingo ndi mitundu yosiyana-siyana ya pemphero.

MILINGO YA PEMPHERO

Pali milingo itatu yopemphera mosweka mtima: kupempha, kufunafuna, kugogoda.

Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo cidzatsegulidwa kwa inu; pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo citseguldwa. (Mateyu 7:7-8).

Kupempha ndi mulingo woyamba wa pemphero. Ndiko kupereka chabe chopempha kwa Mulungu kulandira mayankho mwamsanga. Kuti munthu alandire akuyenera kupempha:

.... mulibe, chifukwa simupempha (Yakobo 4:2).

Pemphero ndi chida chazimu champhamvu kwambiri, koma ambiri sachigwiritsa ntchito. Sapempha, chifukwa cha ichi salandira kanthu.

Kufuna-funa ndi mlingo wina wozamirapo pang'ono. Uwu ndi mlingo umene mayankho sabwera mwamsanga ngati m'mlingo woyamba uja wa kupempha. Okhulupirira zana limodzi ndi makumi awiri omwe anali m'chipinda chapamwamba “anapitirira” m'pemphero ndi chitsanzo cha kufuna-funa. Amuna ndi akazi awa anakhumba kukwaniritsidwa kwa lonjezano la Mzimu Woyera ndipo anapitirira “kufuna-funa” mpaka yankho linafika (Machitidwe 1-2).

Kugogonda ndi mlingo wozama kwambiri. Ndi pemphero lomwe munthu amalimbikabe ndipo mayankho amatenga nthawi kuti abwere. Lafotokozeredwa bwino mu fanizo lomwe Yesu anapereka mu Luka 11:5-10. Mlingo wogogoda ndi mulingo wovuta kwambiri pomenya nkhondo yauzimu m'pemphero. Tikhoza kumvetsa bwino za mulingo wa kugogoda tikaona nkhanu ya Daniel amene analimbikabe kugogoda posatengera kuti sanaone chizindikiro chirichonse chakuti Mulungu wamuyankha Satana atatchinga mayankho ake ochokera kwa Mulungu (Daniel 10).

MITUNDU YA PEMPHERO

Pali mitundu yosiyana-siyana ya pemphero yomwe timaipeza mu pemphero la Ambuye lomwe liri ngati mlozo wathu wa pemphero (Mateyu 6:9-13).

1. Kulambira and matamando:

Timayenera kufika pamaso pa Mulungu ndi kulambira pamodzi ndi kukweza:

(Masalimo 100:4).

Kulambira ndi kupereka ulemu. Kutamanda ndiko kupereka chithokozi poonetsera kuyamika kwa Mulungu pa zomwe watichitira komanso chifukwa cha chimene Iye ali.

Mukuyenera kupembedza Mulungu mu mzimu ndi m'choonadi:

(Yohane 4:23-24).

Malambiro ndi matamando atha kuchitika ndi:

- Kuyimba: Masalimo 9:2,11; 40:3; Marko 14:26

- Matamando omveka: Masalimo 103:1
- Kukuwa: Masalimo 47:1
- Kukweza manja kumwamba: Masalimo 63:4; 134:2; 1 Timoteyo 2:8
- Kuomba m’manja: Masalimo 47:1
- Zida zoyimbira: Masalimo 150:3-5
- Kuimilira: 2 Mbiri 20:19
- Kuwerama: Masalimo 95:6
- Kuvina: Masalimo 149:3
- Kugwanda: Masalimo 95:6
- Kugona pansa: Masalimo 149:5

Womenya nkhondo wa Mulungu mdziko lauzimu amaonekera ndi...

...matamando okweza a Mulungu... mkamwa mwao, ndi lupanga lakuthwa konse konse m’dzanja lawo (Masalimo 149:6).

2. Kudzipereka

Ili ndi pemphero lopereka moyo ndi chifuniro chako kwa Mulungu. Limaphatikizapo pemphero la kudzipereka ndi kudziyeretsa.

3. Kupempha

Ili ndi pemphero lopempha. Zopempha zikuyenera kuperekedwa kwa Mulungu molingana ndi chifuniro chake chomwe chabvumbulutsidwa m’Mau ake. Zopempha zitha kukhala pa milingo ya kupempha, kufuna-funa kapena kugogoda.

4. Kubvomereza ndi kulapa

Pemphero lobvomereza ndilo lolapa ndi kupempha chikhululukiro cha tchimo.

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:9).

5. Kupembedzera

Ili ndi pemphero lopempherera ena. Wopembedzera ndi munthu amene amaima pamaso pa Mulungu m’ malo mwa munthu wina kupempha ndi kudandaulira mavuto ake. Baibulo limanena kuti nthawi ina Mulungu anayang’ana pa dziko lapansi ndipo anaona kuti palibe aliyense yemwe akupembedzera:

Ndipo Iye anaona kuti palibe munthu, nazizwa kuti palibe wopembedzera; cifukwa cace mkono wace wace unadzitengera yekha cipulumutso; ndi cilungamo cace cinamcirikiza. (Yesaya 59:16).

Mulungu ataona kuti palibe wopembedzera, anatumiza Yesu:

Pakuti pali Mulungu mmodzi, ndi Mtetezi mmodzi pakati pa Mulungu ndi anthu, ndiye munthu, Kristu Yesu, (1 Timoteyo 2:5).

ndani adzawatsutsa? Kristu Yesu ndiye amene adafera, inde makamaka, ndiye amene adauka kwa akufa, 10 amene akhalanso pa dzanja lamanja la Mulungu, amenenso atipempherera ife. (Aroma 8:34).

kucokera komwekoakhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa iye, popeza ali nao moyo wace cikhalire wa kuwapembedzera iwo. (Aheberi 7:25)

Yohane 2:1 Tiana tanga, izi ndikulemberani, kuti musacimwe. Ndipo akacimwa wina, Nkhoswe tiri naye kwa Atate, ndiye Yesu Kristu wolungama; (1 Yohane 2:1)

M'bwalo la milandu mumakhala woimilira munthu amene akuimbidwa mulandu, kumulankhulira nkhanu yake. M'nkondo yauzimu, kupembedzera ndi pemphero lopita kwa Mulungu m'malo mwa munthu wina.

Nthawi zina kupembedzera kumachitika ndi chidziwitso. Umapembedzera mu chilankhula chanu:

Ndidandaulira tsono, poyambayamba, kuti acitike mapembedzo, mapemphero, mapembedzero, mayamiko, cifukwa ca anthu onse; cifukwa ca mafumu ndi onse akucita ulamuliro kuti m'moyo mwathu tikakhale odika mtima, ndi acete m'kulemekeza Mulungu, ndi m'kulemekezeka monse. (1 Timoteyo 2:1-2).

Koma nthawi zina kumachitika ndi Mzimu Woyera. Kutha kuchitika ndi kubuula komwe kumabwera chifukwa cha katundu wauzimu wolemera kwambiri. Kutha kuchitika m'malilime osadziwika. Utha kumapembedzera munthu wina kapena Mzimu Woyera kupembedzera iweyo. Zikachitika izi, Mzimu Woyera kudzera mwa inu amalankhula kwa Mulungu molingana ndi chifuniro chake. Mtundu uwu wa pemphero, inu simumvapo kanthu:

Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwiniatipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka; (Aroma 8:26)

Uwu ndi mlingo wozama kwambiri wa pemphero lopembedzera ndipo ndi wamphamvu koposa mu nkondo yauzimu.

MLOZO WA PEMPHERO

Nthawi ina Yesu analandira pempho lochititsa chidwi kuchokera kwa ophunzira ake:

...m’modzi mwa ophunzira ake anati kwa Iye, Ambuye, tiphunzitseni ife kupemphera... (Luka 11:1).

Ophunzirawa sanapemphe za kulalikirira kapena kuchita zozizwa. Sanapemphe kuti aphunzire za kumanga maubwenzi okhazikika. Sanapemphe za kudabwitsa kolandira machiritso a kuthupi. Anapempha kuti aphunzitsidwe kupemphera.

Chidabweretsa njala iyi mwa iwo ndi chiyani? Ndi zomwe zimaonekera pa moyo ndi utumiki wa Yesu chifukwa cha kupemphera. Ophunzira a Yesu anaona zotsatira za pemphero mu nkondo yauzimu zikuchitika.

Tawerangani mlozowu (Mateyu 6:9-13) ndi kuona mitundu ija ya pemphero mwaphuzirayi:

Atate wathu wa kumwamba, Dzina lanu liyeretsedwe	Kulambira ndi kuyamika
Ufumu wanu udze, Kufuna kwanu kuchitidwe monga kumwamba chomwechonso panso pano	Kudzipereka
Mutipatse ife chakudya chathu cha lero	Kupempha
Ndipo mutikhulukire ife zochimwa zathu, monga ifenso tiwakhulukira amangawa athu	Kubvomereza ndi Kupembedzera
Musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse ife kwa woipayo	Kupempha
Pakuti wanu uli Ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemerero kunthawi za nthawi, Amen.	Kulambira ndi matamando

KAPEMPHEREDWE

Onani mavesi onse omwe ali m’musiwa ndipo muone m’mene mungapempherere:

- Pemphero limapita kwa Mulungu: Masalimo 5:2
- Kubwereza bwereza kopanda tanthauzo sikoyenera koma koona mtima: Mateyu 6:7; Daniel 6:10; Luka 11:5-13; 18:1-8
- Mumachimwa ngati simupempherera ena: 1 Samuel 12:23
- Pempherani ndi chidziwitso (chilankhulo chodziwika): Aefeso 6:18
- Pempherani mwa Mzimu: Aroma 8:26; Yuda 20
- Pempherani molingana ndi chifuniro cha Mulungu: 1 Yohane 5:14-15
- Pempherani m’seri: Mateyu 6:6
- Pemphero zomveka ndi moona mtima osati kungochuluka zolankhula: Mateyu 6:7
- Pempherani nthawi zonse: Luka 21:36; Aefeso 6:18
- Pemphero mowirikiza: Aroma 12:12
- Pempherani kosalekeza: 1 Atesalonika 5:17

- Pempherani kwa Atate mu dzina la Yesu: Yohane 15:16
- Pempherani ndi kuyang'anira: 1 Petro 4:7
- Pempherani molingana ndi mlozo wa pemphero: Mateyu 6:9-13
- Pempherani ndi mtima wokhululuka: Marko 11:25
- Pempherani ndi kudzipetsa konse: Mateyu 6:7
- Nthawi zina pemphero lichitike pamodzi ndi kusala kudya: Mateyu 17:21
- Pempherani mosweka mtima: Yakobo 5:16; Akolose 4:12
- Pempherani ndi kugonjera kwa Mulungu: Luka 22:42
- Gwiritsani ntchito njira yomanga ndi yomasula m'pemphero: Mateyu 16:19

ZOMWE MUNGAPEMPHERERE

- Mtendere wa Yerusalemu: Masalimo 122:6
- Ogwira ntchito m'munda: Mateyu 9:38
- Kuti musalowe m'kuyesedwa: Luka 22:40-46
- Omwe akukunyozeni (adani anu): Luka 6:28
- Oyera mtima onse: Aefeso 6:18
- Odwala: Yakobo 5:14
- Wina ndi mnzake (kunyamulirana zothodwetsa wina ndi mnzake): Yakobo 5:16
- Amuna onse, mafumu, ndi iwo amu ulamuliro: 1 Timoteyu 2:1-4
- Zosowa za tsiku ndi tsiku: Mateyu 6:11
- Nzeru: Yakobo 1:5
- Machiritso: Yakobo 5:14-15
- Chikhululukiro: Mateyu 6:12
- Chifuniro cha Mulungu ndi Ufumu wake ukhazikitsidwe: Mateyu 6:10
- Kupumulitsidwa ku mazunzo: Yakobo 5:13

PEMPHERANI MALONJEZANO

Mupempha, ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukacimwaze pocita zikhumbitso zanu. (Yakobo 4:3)

Mulungu amayankha mapemphero molingana ndi malonjezano ake. Mukamapempha mosemphana ndi malonjezanowa, pemphero lanu siliyankhidwa. Zili monga momwe tate akhalira ndi ana ake. Munthu sampatsa mwana wake wamng'ono chirichonse apemphecho. Amaonetsetsa kuti zina zichitike koma zina ayi. Mu njira imeneyi tateyo amapereka zinthu zina mwana akapempha ndipo zina samupatsa.

Izi zili chimodzimidzi ndi Mulungu. Wapereka malonjezano kwa ife ndipo malonjezanowo amatitsogolera momwe tingaperekere zopempha zathu kwa Iye. Mukuyenera kudziwa malonjezano a Mulungu. Mukatero, pempherani molingana ndi malonjezanowo. Njira imodzi yomwe mungatsate pochita izi ndiko kuchekenera malo ena alionse pomwe pali vesi ya

malonjezano. Gwiritsani ntchito Baibulo lanu popemphera molingana ndi mavesi a malonjezano aja.

ZOTCHINGA ZA PEMPHERO

- Tchimo la mtundu uliwonse: Yesaya 59:1-2; Masalimo 66:18; Yesaya 1:15; Miyambo 28:9
- Mafano a mu mtima: Ezekiele 14:1-3.
- Mzimu wosakhulukira: Marko 11:25; Mateyu 5:23
- Kudzikonda, zokhumba zolakwika: Miyambo 21:13; Yakobo 4:3.
- Njala yofuna maudio, mapemphero olakwika: Yakobo 4:2-3.
- Kusakhala bwino ndi wokondedwa wanu: 1 Petro 3:7
- Kudzimva kukhala wolungama: Luka 18:10-14.
- Kusakhulupirira: Yakobo 1:6-7.
- Kusakhala mwa Khristu ndi Mau ake: Yohane 15:7
- Kusowa chifundo: Miyambo 21:13.
- Chinyengo, kunyada, kupemphera mobwereza-bwereza: Mateyu 6:5; Yobu 35:12-13.
- Kusapemphera molingana ndi chifuniro cha Mulungu: Yakobo 4:2-3.
- Kusapempha mu dzina la Yesu: Yohane 16:24
- Zotchinga za ziwanda za Satana: Daniele 10:10-13; Aefeso 6:12.
- Kusafuna kaye Ufumu wa Mulungu: Ndi pokha-pokha mwafuna kaye Ufumu wa Mulungu kuti “zina zonse” zidzakutsatani: Mateyu 6:33.
- Mulungu atha kukhala ndi cholinga chachikulu pa inu pamene akukukanizani zomwe mwapemphazo: 2 Akorinto 12:8-9.
- Mukapanda kudziwa momwe mungapempherere, pemphero limatchingidwa. Apa ndi pomwe pamafunika kumlola Mzimu Woyera kuti apemphere kudzera mwa inu: Aroma 8:26.

NTHAWI YOSAFUNIKA KUPEMPHERA

Ndi bwino kuphunzira kudikira pa Ambuye m’pemphero kuti akutsogolereni musanachite kalikonse. Komanso ndi zofunika kudziwa nthawi yoti simukufunika kupemphera koma kuchita. Mulungu akupatsani mwayi woti muchite kanthu, chitani, osati kupitiriza kupemphera.

Mwa chitsanzo, pa madzi owawa aku ku Mara pamene Mose analilira kwa Ambuye, Mulungu anamuza Mose chochita kuti madzi akhale okoma. Panalibenso chifukwa chomadikira pa Ambuye m’pemphero. Mose anayenera kuchita mwamsanga zomwe Mulungu wabvumbulutsa. Chimodzimodzinso Yoswa, pamene anapemphera za kugonjetsedwa koopsa kwa Israel ndi Ayi. Mulungu anabvumbulutsa kuti pali tchimo pakati pa ana a Israel. Anamuza Yoswa kuti...

Dzuka, ugonerani pansu pa nkhope pako? Israel wachimwa.... Dzuka, yeretsa Israel (Yoswa 7).

Sinali nthawi yopemphera. Inali nthawi yoti achite malangizo omwe wauzidwa m'pemphero ndi Mulungu. Anthu ena amagwiritsa ntchito pemphero ngati pothawira kuti asachitepo kanthu pa zomwe Mulungu wawauza kuti achite.

Enanso amapitirirabe kupemphera koma Mulungu atayankha kale posasangalala ndi yankholo. Onani nkhani ya Balaam mu Numeri 22 makamaka mavesi a 18-22. Balaam analibe chifukwa chokwanira kupita kwa Mulungu ndi yomweyo popeza Mulungu anali atamletsa kale kuti asatengepo pa zomwe zikuchitikazo (onani vesi 12).

KUSALA KUDYA

Kusala kudya ndi gawo lachinayi la nkondo. Kumachitika pamodzi ndi pemphero kumenya nkondo mu dziko lauzimu.

TANTHAUZO LA KUSALA KUDYA

Kusala kudya, tanthauzo losavuta, ndiko kukhala osadya.

MITUNDU YA KUSALA KUDYA

Molingana ndi Mau a Mulungu, pali mitundu iwiri ya kusala kudya. Kusala kwa tunthu ndi kusala moyepula. Kusala kwatunthu ndi pomwe munthu sakudya kapena kumwa chiri chonse (Machitidwe 9:9). Kusala moyepula ndi pomwe munthu amangodyako tina ndi tina basi (Daniel 10:3).

KUSALA KUDYA KOWONEKERA NDI KWA MSERI

Kusala kudya ndi nkhani ya pakati munthu ndi Mulungu. Imachitika mseri osati kumalengeza:

Ndipo Simoni Petro anayankha nati, Inu ndinu Kristu, Mwana wa Mulungu wamoyo. Ndipo Yesu anayankha iye, nati, Ndiwe wodala, Simoni Bar-Yona: pakuti thupi ndi mwazi sizinakuululira ici, koma Atate wanga wa Kumwamba. Ndiponso Ine ndinena kwa iwe, kuti iwe ndiwe Petro, ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazika Mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzaulaka uwo. (Mateyu 6:16:18).

Atsogoleri atha kulengeza dongosolo losala kudya la mpingo wonse:

Ombani lipenga m'Ziyoni, patulani tsiku losala, lalikirani msonkhano woletsa, (Yoweli 2:15).

CHOLINGA CHA KUSALA KUDYA

Pali zolinga zeni zeni zauzimu zosalira kudya. Nkofunika kumvetsa bwino zimenezi, popeza ngati musala kudya ndi zolinga zolakwika simupindula kanthu.

Werengani mavesi ali m'musiwa pa zolinga zosalira kudya. Mavesiwa amabvumbulutsa mphamvu yodabwitsa ya kusala kudya mu nkondo yauzimu. Munthu amasala kudya kuti:

- Adzichepetse yekha: Masalimo 35:13; 69:10
 - Alape matchimo: Yoweli 2:12
 - Kuti mulandire bvumbulutsa: Daniel 9:2; 3:21-22
 - Kumasula magoli a uchimo, kuchotsa zolemetsa, kumasula amsinga, kuphwanya magoli: Yesaya 58:6
 - Kudyetsa osauka kuthupi ndi kuuzimu komwe: Yesaya 58:7
 - Kuti pemphero limveke kwa Mulungu: 2 Samueli 12:16,22; Yona 3:5,10.
- Kusala kudya sikumasinthwa Mulungu. Imasinthwa inu. Mulungu amachita nanu molinga ndi ubale womwe muli nawo ndi Iye. Mukasinthwa, machitidwe a momwe Mulungu amachitira ndi inu adzasinthanso. Simusala kudya kuti musinthe Mulungu, chifukwa Mulungu sasinthwa. Werengani bukhu la Yona kuti muone momwe izi zinachitikira ku Nineve.

KUTALIKA KWA NTHAWI YOSALA KUDYA

Kutalika kwa nthawi yosala kudya kumatengera momwe Mulungu walankhulira mu mtima mwanu. Mulungu angathe kukutsogolerani kuti musale nthawi yochepa kapena yaitali. Kumbukirani nkhani ya Esau ndi Yakobo. Yakobo amaphika chakudya choti adye koma ataona kuti pali mwayi wotenga ukulu, analolera kupereka chakudya ndi kukhala ndi njala. Kodi Esau akanasala chakudya chimenechi sizikanakhala bwino kodi?

MFUNGULO ZA UFUMU

Yesu anapereka mfungulo za Ufumu. Mfungulo zimenezi ndi kuphatikizapo mphamvu yomanga ndi kumasula ndipo ndi gawo lachisanu la dongosolo lathu la nkondo:

Ndidzakupatsa mafungulo a Ufumu wa Kumwamba; ndipo cimene ukamanga pa dziko lapansi cidzakhala comangidwa Kumwamba: ndipo cimene ukacimasula pa dziko lapansi, cidzakhala comasulidwa Kumwamba. (Mateyu 16:19).

Yesu anaphunzitsa za ubwino wakumanga mizimu yoipa musanaisamutse, koma mfundo ya kumanga ndi kumasula imaposa kusamutsa ziwanda. Mutha kumanga mphamvu za ntchito za mdani pa moyo wanu, m'nyumba mwanu, mdera lanu, ngakhale mu mpingo mwanu. Mutha kumasula amuna ndi akazi ku mphamvu ya uchimo, kusakondwa, ndi kufooketsedwa ndi mdani.

Mfundo ya kumanga ndi kumasula ndi njira yofunika kwambiri pogonjetsa mphamvu za mdani. Ndi mfungulo ya mu Ufumu wa Mulungu. Mu nyengo ina iriyonse yomwe mukukumana nayo, kaya ndi vuto la mtundu wanji, iri ndi mfungulo yauzimu. Mfungulo yake ndiyo kugwiritsa

ntchito njira ya kumanga ndi kumasula. Mukazindikira choti mumange ndi choti mumasule, pamenepo, mdani adzakhala wogonjetsedwa.

DZINA LA YESU

Gawo lomaliza la dongosolo la nkhondo yathu likupezeka mu dzina la Yesu. Mau a Mulungu akuyenera kugwiritsidwa ntchito mu dzina lake, kupemphera, kusala kudya, ndi kugwiritsa ntchito mphamvu ndi ulamuliro wopatsidwawu komanso mfungulo za mu Ufumu mu dzina lake.

Ngati mudzapempha kanthu m'dzina langa, ndidzacita. (Yohane 14:14)

Ndipo tsiku limenelo simudzandifunsa kanthu. Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Ngati mudzapempha Atate kanthu, adzakupatsani inu m'dzina langa. (Yohane 16:23)

Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalangidwa. Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Mark 16:17-18)

Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:18-20)

Mukuyenera kuphunzitsa, kubatiza, kusamutsa ziwanda, kuchiritsa odwala, ndi kugonjetsa mphamvu iriyonse ya mdani kudzera mu dzina la Yesu. Ndi la mphamvu kwambiri kuposa dzina lina liri lonse.

pamwamba pa ukulu wonse, ndi ulamuliro ndi mphamvu, ndi ufumu, ndi dzina liri lonse lochedwa, si m'nyengo yinoya pansi pano yokha, komanso mwaiyo ikudza;(Aefeso 1:21)

Mwa icinso Mulungu anamkwezetsa iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse, kuti m'dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m'mwamba ndi za padziko, ndi za pansi pa dziko, ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate. (Afilipi 2:9-11)

NJIRA YOPAMBANIRA

Yesu anakumana ndi yesero liri lonse lomwe tikukumana nalo koma anagonjetsa mayesero onsewo osachimwa. Chifukwa chakuti analowako mu gawo la nkondo yauzimu, amamvetsetsa nkondo zanu ndipo amakulimbikitsani:

Pakuti sitiri naye mkulu wa ansebe wosatha kumva cifundo ndi zofoka zathu; koma wayesedwa m'zonse monga momwe ife, koma wopanda ucimo. (Ahebri 4:15)

Chifukwa chakuti Iye anagonjetsa, inunso mutha kukhala mgonjetsi:

Mudagonjetsa zonse pansu pa mapaziace. Pakuti muja adagonietsa zonse kwa iye, sanasiyapo kanthu kosamgoniera iye. Koma sitinayamba tsopano apa kuona zonse zimgonjera. (Ahebri 2:8).

Werengani nkhani ya imfa ndi kuuka kwa Yesu mu Mateyu 26-28; Marko 14-16; Luka 22-24; ndi Yohane 18-21. Imfa ndi kuuka kwa Yesu inali yaikulu yoopsa yomwe inachitikapo pakati pa mphamvu ya Mulungu ndi mphamvu ya Satana.

Kudzera mu imfa ya Yesu, Satana amaganiza kuti wakwanitsa kuononga dongosolo la Mulungu. Wapha Mwana wa Mulungu m' modzi yekha. Waononga mfumu yomwe imayenera kulamulira Ufumu wa Mulungu. Koma Yesu anati:

Uganiza kuti sindingathe kupemphera Atate wanga, ndipo Iye adzanditumizira tsopano lino mabungwe a angelo oposa khumi ndi awiri? Koma pakutero malembo adzakwaniridwa bwanji, pakuti kuyenera comweco? (Mateyu 26:53-54).

Cifukwa cace ngati Mwana adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu. (Yohane 18:36).

Yesu anamyankha iye, Simukadakhala nao ulamuliro uli wonse pa Ine, ngati sukadapatsidwa kwa inu kucokera Kumwamba; cifukwa ca ici iye wondipereka Ine kwa inu ali nalo cimo loposa. (Yohane 19:11).

Yesu sanafe chifukwa chakuti mphamvu yake inali yoperewera poyerekeza ndi mphamvu za mdaniyo ayi. Imfa ya Yesu sinathetse dongosolo la Ufumu wa Mulungu. Siinali nthawi yake kuti Ufumu wake ukazikitsidwe pa dziko lapansi.

M'malo mwake imfa ya Yesu inakwaniritsa dongosolo la Mulungu. Anthu tsopano akutha kupulumutsidwa ku gori la uchimo ndi chilango cha “imfa yachiwiri” (kusiyanana ndi Mulungu kwamuyaya chifukwa cha uchimo).

Ngakhale izi ziri zazikulu koposa, kupulumutsidwa ku uchimo sichinali chigonjetso chokhacho chomwe chinapezeka kudzera mu imfa ya Yesu pa mtanda ayi. Kudzera mu imfa yake ndi kuuka kwake, Yesu anagonjetsa mphamvu zonse za mdani:

cimene anaticurukitsira ife m'nzeru zonse, ndi cisamaliro. Anaticurukitsira ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anaticurukitsira mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 4:8-10).

atabvula maukulu ndi maulamuliro, anawaonetsera poyera, nawagonjetsera nako. (Akolose 2:15).

Yesu anagonjetsa mphamvu zonse za mdani kuphatikizapo imfa. Anaperekanso chiweruzo pa Satana:

Filipo anadza nanena kwa Andrey; nadza Andrey ndi Filipo, nanena ndi Yesu. Tsopano pali kuweruza kwa dziko ili lapansi; mkulu wa dziko ili lapansi adzatayidwa kunja tsopano, (Yohane 12:31).

Yesu anakonza njira ya chipulumutso. Anagonjetsa imfa komanso maukulu ndi mphamvu za mdani. Anabwezeretsa ulamuliro pa zinthu zonse kwa munthu. Analengeza chilango kwa Satana chomwe chidzakwaniritsidwe mtsogolomu.

Monga momwe mwaphunzilira, zimene tikukambazi zikufanana ndi zomwe zimachitika ngakhale kuthupi m' maiko ena pa dziko lapansi. Mphamvu ya zigawenga zitha kugonjetsedwa ndi asilikari a boma. Mtsogoleri wa zigawenga nkuweruzidwa kuti ndi wolakwa koma adakali chothawa. Komabe asilikari ake amakhala akumenyabe nkondo m' dzikomo molamulidwa ndi iyeyo.

Yesu wagonjetsa Satana ndipo waikiratu chilango chake, koma adakali wothawa-thawa ndipo mphamvu zake za ziwanda, thupi, ndi dziko zikumenyabe nkondo m' dziko. Akuyesera kulamulira dera lomwe ndi Wogonjetsayo. Akuyesetsa kupanga anthu kusazindikira kuti Satana ndi wogonjetsedwa ndipo ali pansu chiweruzo cha Mulungu. Amayesetsa kumalamulira nyumba, mipingo ndi maiko.

Apa ndi pomwe nkondo ya wokhulupirira imaonekera. Yesu anagonjetsa mdaniyo koma Satana adakali wothawa-thawa pa dziko lapansi. Ndi ntchito yathu kutsegula maso a amuna ndi akazi kuzindikira za chinyengo chake ndi kutenganso ulamuliro ku madera omwe ndi athu.

Nkondo ya inu ngati munthu payekha, ipilirabe kufikira chiweruzo pa Satana chachitika kapena kufikira mutapita kwa Ambuye kudzera mu imfa, chomwe chiyambecho.

kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m' zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu, (Aefeso 3:10).

OGONJETA, OSATI OGONJETSEDWA

Kudzera mwa Yesu, inu ndi ogonjetsa osati ogonjetsedwa ndi mdaniyo:

Anakonza zonse pansi pa mapazi ace, nampatsa iye 4 akhale mutu pamtu pa zonse, 5 kwa Eklesia amene ali thupi lace, 6 mdzazidwe wa iye amene adzazazonse m'zonse. (Aefeso 1:22-23).

Zinthu zonse ziri “pansi pa mapazi” a Yesu. Kutanthauza kuti wazigonjetsa. Iye ndi mutu wa Mpingo ndipo ife ndi thupi. Zalembedwa kuti zinthu zonse ziri pansi ku mapazi ake, kutanthauza kuti pansi pa Thupi lake, lomwe ndi Mpingo. Izi zikutanthauza kuti ife ndi ogonjetsa osati ogonjetsedwa. Mutha kutetezedwa ku mphamvu za Satana. Yesu mwini anatipempherera ife kuti titetezeke ku mphamvu za mdaniyo:

Sindipempha kuti muwacotse iwo m'dziko lapansi, koma kuti muwasunge iwo kuletsa woipayo. Koma sindipempherera iwo okha, komanso iwo akukhulupirira Ine cifukwa ca mau ao; (Yohane 17:15, 20).

Inu ndinu wogonjetsa, osati kudzera mphamvu zanu, koma kudzera mu mphamvu za Wamkuluyo:

Komam'zonsezi, ife tilakatu, mwa iye amene anatikonda. (Aroma 8:37).

Pamene nkondo yauzimu yafika popweteka, kumbukirani kuti Baibulo limatitsimikizira kuti zolinga za Mulungu zidzakwaniritsidwa:

Yehova wa makamu walumbira, nati, Ndithu monga ndaganiza, coteru cidzacididwa; ndipo monga ndapanga uphungu, coteru cidzakhala; (Yesaya 14:24).

Umenewu ndi uphungu wopangira dziko lonse; ndipo ili ndi dzanja lotambasulidwa pa amitundu onse. Pakuti Yehova wa makamu wapanga uphungu, ndani adzauleketa? ndi dzanja lace latambasulidwa, ndani adzalibweza? (Yesaya 15:26-27).

Ambuye wa makamu ali ndi cholinga, ndipo palibe mphamvu ya dziko lapansi, Gahena kapena Satana, yomwe idzalepheretsa.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za NKhondo.

2. Kodi cholinga cha Mulungu ndi chiyani?

3. Nchifukwa chiyani Yesu anabwera pa dziko lapansi?

4. Kodi dongosolo la nkhondo lokhala ndi mfundo zisanu ndi imodzi ndi lotani?

(Mayankho a mafunso awa ali kumapeto a bukhu lino)

MACHITA-CHITA A LUSO

1. M'phuziro lino mwaphunzira za kufunika kwa Mau a Mulungu pa nkhondo yauzimu. Harvestime International Institute imapereka maphunziro awiri omwe awonjezere kuthekera kwanu kogwiritsa ntchito Mau a Mulungu. Maphunzirowa ndi "*Kusanthula Baibulo Mwaluso*" ndi "*Kafuku-fuku wa Baibulo.*"
2. M'phunziro lino mwaphunzira kuti Yesu anabwera kudzaononga ntchito za Satana. Werengani zambiri za zolinga za Yesu m'mavesi ali m'musiwa: Luka 4:18-19; 4:43; 19:10; 24:46-49; Yohane 6:38; 9:4; 12:46; 18:37. Werengani za zolinga za Mulungu mwa Yesu: Yohane 3:16:18; Aefeso 1:9-10.
3. Yesu anakumana ndi kulimbana ndi mizimu yoipa. Komano mizimu yoipa ndi mayesero a Satana si nkhondo zokhazo zomwe Yesu anamenyana nazo. Satana anagwiritsanso ntchito anthu omwe anali pafupi ndi Yesu kulimbana naye:

Petro:

Simon Petro anali m'modzi mwa ophunzira omwe Yesu anawasankha koma Petro nthawi zina anali kugwiritsidwa ntchito kulimbana ndi naye. Yesu atangobvumbulutsa za imfa yake yomwe imabwera patsogolo, Petro anayamba kumdzudzula kuti sanachite bwino kulankhula zimenezo (Marko 8:32). Yesu anamuuza Petro kuti:

Koma Iye anapotoloka, napenya ophunzira ace, namdzudzula Petro, nanena, Coka, pita kumbuyo kwanga, Satana iwe; popeza susamalira zinthu za Mulungu, koma za anthu. (Marko 8:33)

Yesu samatanthauza kuti Petro ndi Satana, koma kuti Petro amagwiritsidwa ntchito ndi Satana pa nthawi imeneyo.

Imodzi mwa njira zomwe Satana amazidalira ndiyogwiritsa ntchito anthu omwe amakhala pafupi nanu kukutchingani kuti musachite chifuniro cha Mulungu. Monga momwe Yesu anachitira, mukuyenera kuwakankhira kumbuyo kwanu. Kodi Satana akugwiritsa ntchito munthu wina yemwe ali pafupi nanu kukutsekerezani kuti musachite chifuniro cha Mulungu?

Patsogolo pake, pamene Petro analonjeza kukhala pambuyo pa Ambuye, Yesu anati kwa iye:

Simoni, Simoni, taona, Satana anafunsa akutengeni kuti akupeteni ngati tirigu; koma ndinakupempherera kuti cikhulupiriro cako cingazime; ndipo iwe, pamene watembenuka ukhazikitse abale ako. (Luka 22:31-32).

Yesu anadziwa kuti nthawi yakupachikidwa kwake ikayandikira, Petro adzamukana. Anaoneretu momwe Satana anakonzera kuchotsa chabwino chirichonse mwa Petro. Koma Yesu amaonanso utumiki waukulu mwa Petro. Amadziwa kuti tsiku lina Petro adzakhala mtsogoleri wamphamvu kwambiri mu mpingo woyamba.

Yudasi:

Yudasi anali m' modzi mwa ophunzira oyambilira a Yesu. Yesu anadziwiratu pachiyambi momwe Satana adzagwiritsire ntchito Yudasi:

(Yohane 6:70-71).

Werengani za kuperekedwa kwa Yesu ndi Yudasi mu Mateyu 26:20-25 ndi Yohane 13:21-30. Kodi Satana wagwiritsa ntchito anthu apafupi kukuikani m' mavuto ndi kukuvulazani? Monga Yesu anachitira, musamulole iye akutchingeni ku cholinga chomwe Yesu wakuikirani.

4. Werengani Malaki 1:13. Mneneri akufotokozera kuti mu nthawi yake anthu ena anali kuipidwa ndi zofunikira pachipembedzo. Mwina anthuwa sanaphunzire bwino momwe angapembedzere?

Werengani zambiri za kupembedza: Masalimo 5:7; 22:27; 29:2; 45:11; 66:4; 86:9; 95:6; 96:9; 97:7; 99:5,9; Eksodo 34:14; 1 Mbiri 16:29; Mateyu 15:9; Marko 7:7; Yohane 4:23-24; Afilipi 3:3.

Harvestime International Institute ili ndi phunziro lotchedwa “Ndongomeko Zosonkhanitsira” lomwe liri ndi malangizo ambiri pa kapembedzedwe.

5. Werengani zambiri za matamando m’buku la Masalimo. Ikani chizindikiro pa mau onse olembedwa “matamando” paliponse mungawaone kenako bwelerani muyambe kusanthula mavesi amenewo.

6. Zinthu zina zokhuza pemphero nazi:

Mayankho a mapemphero amaperekedwa:

Pena nthawi yomweyo: Yesaya 65:24; Danieli 9:21-23

Pena mochedwa: Luka 18:7

Pena mosemphana ndi zokhumba zathu: 2 Akorinto 12:8-9

Mopilira chiyembekezo chatu: Yeremiya 33:3; Aefeso 3:20

Makhalidwe osiyana-siyana ogwiritsidwa ntchito popemphera:

Kuimilira: 1 Mafumu 8:22; Marko 11:25

Kuwerama pansu: Masalimo 95:6

Kugwada: 2 Mbiri 6:13; Masalimo 95:6; Luka 22:41; Machitidwe 20:36

Kugwa nkhope pansu: Numeri 16:22; Yoswa 5:14; 1 Mbiri 21:16; Mateyu 26:39

Kutambasula manja: Yesaya 1:15; 2 Mbiri 6:13

Kukweza manja kumbamba: Masalimo 28:2; Maliro 2:19; 1 Timoteyo 2:8.

Mavuto omwe mukuyenera kuthana nawo kuti mupemphere:

Kusowa kwa nthawi

Zosokoneza

Kutopa

Kusowa chidwi

Kusonkhanitsa Mphamvu za Pemphero

Pemphero ndi chimodzi mwa zida zodalirika kwambiri- mu nkondo yauzimu. Chipangano Chatsopano chili ndi dongosolo la momwe mungapangire kuti mapemphero anu akhale a mphamvu:

Pemphero la panokha: Pemphero lamseri la munthu payekha: Mateyu 6:6.

Anthu awiri kupemphera pamodzi: Kupemphera limodzi anthu awiri ndi gawo laling’ono kwambiri la pemphero la gulu: Mateyu 18:19.

Timagulu ting’onoting’ono: Timagulu iti timakhala ndi anthu oposa awiri kubwera pamodzi m’pemphero. Pali mphamvu zazikulu pamene anthu awiri kapena atatu agwirana manja pa cholinga ichi: Mateyu 18:20.

Pemphero la mpingo wonse: Mpingo wonse ukuyenera kubwera pamodzi nthawi za mapemphero a gulu: Machitidwe 1:14-15

Malonjezo a Pemphero

Werengani malonjezo otsatirawa a mapemphero. Amabvumbulutsa mphamvu za chida champhamvuchi mu nkondo yauzimu:

- Atate amadziwa zomwe mukusowa ngakhale musanayambe kupempha: Mateyu 6:8
- Ngati anthu awiri angagwirizane m'pemphero, lidzayankhidwa: Mateyu 18:19
- Zinthu zonse ndi zotheka ndi Mulungu: Mateyu 19:26; Luka 18:27
- Pemphero lophatikizana ndi chikhulupiriro limakhala lamphamvu: Mateyu 21:22; Marko 11:24
- Pemphero la munthu wolungama limachita kwakukuru: Yakobo 5:16
- Mukapempha mu dzina la Yesu, zidzachitika: Yohane 14:14

Phunzirani zambiri za kusala:

- Kusala kudya ndi chimodzi mwa zinthu zomwe zimatiyenerereza ife ngati atumiki a Mulungu: 2 Akorinto 6:3-10.
- Pemphero ndi kusala kudya zimagwiritsidwa ntchito m'mayendetsedwe a mpingo: Machitidwe 14:23
- Tikuyenera kudzipereka ku moyo “wakusala kudya”: 1 Akorinto 7:5

Yesu ananena kuti mudzakhala ndi yoponda pa “njoka ndi zinkhanira.” Mu Chaputala 5 munaphunzira za momwe makhalidwe a njoka amafananira ndi machitachita a Satana. Izi ndi zina za makhalidwe a zinkhanira mu uzimu:

Zinkhanira zemalewa ena. Chinkhanira chimalimbana ndi mdani mpaka chife. Imagwira mdani chakudya chake, kuphwanya, ndikufinyira mphamvu yake ya ululu. Ukalumidwa ndi chinkhanira, umamva kupweteka, umavutika kulankhula, umasowa mtendere, umafooka, komanso dzanzi.

Zinkhanira zimakonda malo a mdima ndipo zikaona kutentha zimafa. Poyamba zimathawa, kenako zimayamba kukalipa ndi mchira wake. Nyerere zimadana kwambiri ndi zinkhanira.

Kodi mungathe kuyerekeza makhalidwe a zinkhanira ndi moyo wauzimu monga momwe tinachitira ndi njoka mu Chaputala 5?

KUKUSA

NTCHITO YAIKULU YA USILIKARI MGULU LA NKHONDO LA MULUNGU

“Kukusa” kumatanthauza kupanga gulu kukhala la lokonzeka kumenya nkhondo. “Kukusa” ndi ntchito yoikidwa m’ malo momwe msilikari aime ngati mbali imodzi ya mphamvu zauzimu zagulu la nkhondo la Mulungu.

CHAPUTALA 10

NKHONDO YOIPALAMULA NDI YODZITETEZA

ZOLINGA

Mukamaliza chaputala chino mutha kukwanitsa:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kutanthauzira mau oti “nkhondo yoipalamula.”
- Kutanthauzira mau oti “nkhondo yodzitetezera.”
- Kuzindikira chinthu chofanana pakati pa nkhondo ziwirizi.
- Kulemba mwachidule ntchito ya Mzimu Woyera mu nkhondo yoipalamula ndi yodzitetezera.
- Kugwiritsa ntchito luso la masewera omenyana kuti mufotokozere njira zogwiritsa ntchito mu nkhondo yoipalamula ndi yodzitetezera.

VESI LOTSOGOLERA

Ndipo musampatse mpata mdierekezi. (Aefeso 4:27).

MAU OYAMBA

Mdziko la kuthupi kuli mitundu iwiri ya nkhondo: Yoipalamula ndi yodzitetezera. Baibulo limatiphunzira njira zauzimu zomenyera nkhondo zonse ziwiri. Mukuyenera muphunzire kamenyedwe ka nkhondo yoipalamula ndi yodzitetezera. Kuthawa pa nkhoodoyi nkosavomerezeka.

Phunziro lino likutipatsira zofunika kudziwa pa nkhondo yopalamula ndi yodziteteza. Ma chaputala awiri otsatirawo akufotokozera tsatane-tsatane zida zauzimu mu nkhondo zonsezi.

NKHONDO YODZITETEZERA

Nkhondo imeneyi imamenyedwa pofuna kuteteza dera. Ndi nkhondo yomwe imachitika pamene mdaniyo wayamba kuthira nkhondo gulu lina, pamenepo gululo limasonkhanitsa mphamvu zake pamodzi kuti liteteze dziko lake. Wotetezayo amachitapo kanthu pa zomwe mdaniyo akuchita ndipo ziganizo zake zimatengera momwe mdaniyo akuchitira. Nkhondo ngati iyi siyifunika kulimbira kulowa mu dera la mdaniyo. Koma imamenyedwa pofuna kuteteza dera lomwe lalandidwa kale. Izi ndi zofunika kudziwa chifukwa nthawi zonse mphamvu zakumdima zimakhala zikulimbana ndi moyo wa munthu wokhulupirira. Ngati zimukudziwa momwe mungadzitetezere, ndiye basi muthera pompo.

NKHONDO YOPALAMULA

Nkhondo iyi imakhala yoopsa kwambiri. Siikhala nkhondo yodikira kuti mdani akuyambeni ndiye muyambepo kutakataka ayi. Ndi nkhondo yomwe m'makonza dongosolo kuti mukaiyambe. Mumayamba ndi kudziwa mdani wanu, njira zake kenako mumanyamuka kukamthira nkhondo muuzimu. Mu mtundu uwu wa nkhondo, woyambitsayo amakhala ndi mwayi woganiza choti achite poyamba. Nkhondo yopalamula imalanda dera osati kuliteteza.

Kumenya nkhondo ya mtundu uwu ndi komwe kupangitse kuti madera ambiri a dziko lapansi afikiridwe ndi Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. Tisangokhala m'zinyumba ndi m'mipingo yathu chete ndi kumangomenya nkhondo yodzitetezera ayi. Asilikari a Mulungu akuyenera kupita ndi kukalowa m'dera la mdani. Apite komwe kuli malimba a Satana ndi mphamvu ya Uthenga Wabwino. Tikuyenera kumenya nkhondo yauzimuyi mosanyengelera.

CHINTHU CHOFANANA

Pali chintu chimodzi chomwe chimapezeka mu nkhondo zonse ziwiri tatchulazi. Zonsezi zimafuna okhulupirira akhale wa machawi. Kuthupi, zida zosagwiritsidwa ntchito sizingavulaze mdani kapena kupambanitsa pa nkhondo. Chimodzimodzinso ku uzimu. Momwe zida zanu zikhalire zitengera kuti mumazigwiritsa ntchito bwanji. Inde Mulungu amatipatsa mphamvu zomenyera nkhondo koma zitengera inuyo kutengapo mbali pa njira zomenyera nkhondo yauzimu yopalamula kapena yodziteteza.

Mu nkhondo za m'Chipangano Chakale, Mulungu amamenyera nkhondo anthu ake, Israel, pomenya nawo limodzi. Komano Aisraeli amayenera kuti akapezeke ku malo omenyera nkhondoko. Mulungu akaona chida cha nkhondo chikugwiritsiwa ntchito mu dzina lake komanso kuona amuna ndi akazi ataima molimba mtima kufuna kulimbana ndi mdaniyo, Ambuye wa Makamu amalowererapo.

Werengani nkhani ya Elisa mu 2 Mafumu 13:14-19. Mu phunziro ili logwiritsa ntchito uta ndi mivi tikuona kuti pali kufanana kwauzimu komwe kungakuthandizeni kumvetsa bwino mbali yanu mu nkhondoyi:

1. WONETSANI MTIMA WOFUNA KUMENYA NKHONDO

Elisa anauza Mfumu Yoasi, “Tenga uta ndi mivi.” Paulo anati, “Tengani lupanga la Mzimu” ndi kulengeza nkhondo. Pongonyamula zida zanu pokhapo, zikuonetsera kuti muli ofuna kumenya nkhondo.

2. IKANI MANJA ANU PA CHIDACHO:

Elisa anauza Yoasi kuti aike manja ake pa uta, ndipo anaika manja ake pa manja a mfumu. Njira ya chigonjetso ndiyoika manja ako pa chida ndi dzanja la Mulungu pa iwe.

3. TSEGULANI ZENERA

Tsegulani zenera la malo omwe mdani akupambana. Mdani wa Israel anali kuzambwe ndipo Elisa anauza mfumu kuti atsegula zenera lakuzambwe. Mulungu akufuna kuti mutsegule “mazenera” kuti muike poyera kulephera, kugonjetsedwa, ndi ukapolo wa mdaniyo.

4. PONYANI MUVI

Elisa anauza mfumu kuti iponye muvi ndipo mfumu inaponya. Ndipo Elisa anati, “Muvi wa Ambuye wa chigonjetso pa Asiriya.” Mutha kutsegula zenera mutagwira chida mdzanja lanu koma zonse ndi zosakwanira. Ngakhale dzanja la Mulungu liri pa mkono wanu silipambana nkhondo. Mukuyenera kumvera lamulo la Wamkulu wa Nkhondo ndikuponya muvi. Gawo lanu pa nkhondo ndi limeneli... Kugwiritsa ntchito chida chomwe muli nacho mdzanja lanu motsogozedwa ndi dzanja lake.

5. DZIWANI CHOLINGA

Elisa anauza Mfumu kuti itenge mivi ndi kuimenyetsa pansi ngati chigonjetso pa Asiriya. Ndipo mfumu inatero koma inangomenyetsa pansi katatu kokha basi ndikuleka. Elisa anamuuza anamdzudzula kuti waika malire pa kuthekerera kwa Mulungu pomenya katatu kokha, chigonjetso chakenso chiikidwira malire. Izi zinachitika chifukwa chakuti amfumu zanamvetse cholinga cha nkhondo. Elisa anali atatena kuti Mulungu akufuna kuonongeratu mdani (17). Pomenya pansi katatu kokha, ndiye kuti mfumuyi imafuna chigonjetso chochepa.

Cholinga cha Mulungu pa inu ndicho chigonjetso mgawo liri lonse la moyo ndi utumiki wanu. Mukakanika kumvetsa cholinga chimenechi ndiye kuti chigonjetso chanu chikhala chosakwanira.

6. MUPAMBANE KAYE M'TSERI

Zotsatira za nkhondo ndi Asiriya zinatengera zomwe zinachitika mkachipinda kaja pakati pa Elisa ndi Mfumu Yoasi. Chimodzimodzinso ndi nkhondo yauzimu, chigonjetso chanu m'nkhondo yomwe mukumenya chimatengera zomwe zimachitika pakati pa inu ndi Yesu m'tseri.

NJIRA ZA SATANA

Chofunika kwambiri pa nkhondo zonse ziwiri ndiko kudziwa njira zomwe Satana amagwiritsa ntchito:

kuti asaticenierere Satana; pakuti sitikhala osadziwa macenjerero ace.(2 Akorinto 2:11).

Mau akuti “njira” amanthauza dongosolo kapena machenjerero la makhalidwe oipa. Satana atha kukupezelerani mukapanda kudziwa njira zake ndi kulephera kumenya nkondo yopalamula komanso yodziteza.

UTUMIKI WA MZIMU WOYERA

Kumayambiro a phunziro lino munaphunzira za mphamvu ya kuunika ya Mzimu Woyera. Mzimu Woyera ndi wofunika pa nkondo yoipalamula komanso yodziteza. Iye amadziwa machenjerero a Satana ndipo amapempherera okhulupirira omwe akumenya nawo nkondoyi:

Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwiniatipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka; ndipo iye amene asanthula m'mitima adziwa cimene acisamalira Mzimu, cifukwa apempherera oyera mtima monga mwa cifuno ca Mulungu. (Aroma 8:26-27).

Mzimu Woyera amapereka mphamvu zoti mugwiritse ntchito polanda dera la Satana:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Machitidwe 1:8).

Mphatso za Mzimu Woyera ndi zida zamphamvu mu nkondo yopalamula ndi yodziteza. Mphatso ya mau a chidziwitso ndi mau anzeru imapereka bvumbulutso mu nkondo yauzimu. Mphatso yakuzindikira mizimu imabvumbulutsa chinyengo cha mdani.

Mphatso zapadera monga abusa, aneneri, atumwi, alaliki ndi aphunzitsi zimatithandizira mu nkondo yauzimu. Mphatso zolankhula za Mzimu Woyera zimapereka malamulo a padera kuchokera kwa Mulungu ndipo mphatso zotumikira za Mzimu zimapanga gulu la asilikari a Mulungu kumenya nkondo mwa mphamvu.

MASEWERO OMENYANA: FANIZO LA KUTHUPI LA NKHONDO YAUZIMU

Imodzi mwa mavesi a mphamvu kwambiri pa nkondo yauzimu yopalamuala ndi...

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

Masankhidwe a Mulungu pa mau oti, “kumenyana” ndi ofunika kwambiri. Masewero omenyana ali ndi zofanana zambiri ndi nkondo yauzimu. Masewerowa amafunika luso la kagwiritsidwe ntchito ka mphamvu. Uku ndi kulimbana kofuna kuona kuti wamphamvu ndi ndani.

Onani zinthu zili m'musizi zomwe zimafunika kwa munthu wochita masewera omenyana:

1. KUPHUNZIRA KOKONZEKERA

Munthu wochita masewera omenyana amafunika kukonzekera bwino, kudya bwino komanso kutsata malamulo a masewerowo kuti apambane.

Okhulupirira akuyeneranso kudziwa ndi kutsata malamulo a nkondo yauzimu kuti apambane. Kudya Mau a Mulungu pamodzi ndi pemphero ndi kofunika kuti tipambane pa kumenya nkondo yauzimu. Monga m'mene masewera omenyana amakhala, munthu amakhala waluso mu nkondo pamene akukonzekera mokwanira pafupi pafupi.

2. MTUNDU WA NKONDO

Masewera omenyana safunika gulu amachitika ndi munthu m'modzi basi. Akatopa, palibenso wina woti atha kulowa m'malo mwake. Kumakhala kulimbana ndi mdani wekha kukumana naye maso ndi maso. Izi zili chomwecho mu nkondo yauzimu. Okhulupirira amakhala pa nkondo yaokha, kulimbana ndi mdani kukumana naye maso ndi maso. Wokhulupirira wina sangabwere kuti akulandireni kumenya nkondo yauzimuyi. Simukhalanso kupumira ngati m'mene amachitira masewera enawa ayi. Nkondo yauzimu ilibenso kupumulira. Satana sapuma pa nkondoyi. Wokhulupirira akuyenera kukhala maso nthawi zonse.

3. NJIRA ZOMENYERA NKONDO

M'masewera omenyana mumakhala njira zogwiritsa ntchito pomushosha mdani kapena kudziteteza. Ndipo njira zimenezi zingathe kugwiritsidwa ntchito mu nkondo yauzimu. Njira ina ndi yongoima chiriri. Apapa ndi pomwe ukuonetsa kusafuna kukumana ndi mdani wako. Munthu amalephera chifukwa cha kuzemba zemba mdani wake. Mu nkondo yauzimu, munthu amaluzamapointi akamazemba kukumana ndi mdani wake mwamphamvu kuti apambane.

4. KUM'BALALITSA MDANI

Njira ina yopambanira mu masewera omenyana ndi kubalalitsana. Ukam'balalitsa mdani zochitika, amasowa chochita ndipo amalimbana nkuti abwerelemo.

Baibulo limakamba zambiri za kufunika kokhala wodekha. Njira ina yomwe Satana amagwiritsa ntchito muuzimu ndi kubalalitsa. Zipembedzo zambiri zachinyengo zabadwa chifukwa chifukwa cha kubalalika m'chiphunzitso choona. Nyumba zambiri, mipingo ngakhale maiko agonjetsedwa chifukwa chosokonekera mu zochitika nkumalimbana ndi zinthu zosafunika kulimbana nazo kusiya kulimbana ndi zofunika.

Pali magawo awiri a kubalalika mu masewera omenyana: kubalalika m'thupi ndi kubalalika m'maganizo. Wosewera m'modzi amayamba kubalalitsa m'nzake m'maganizo kenaka amadzachita zimene akufuna. Kutu izi zitheke amam'dzidzimutsa winayo kuti amjejemetse. Pamene winayo akuganiza kuti apewe basi amangokumana ndi chibakera.

Izi ndi zomwe Satana amachita. Amadzidzimutsa munthu ndi cholinga chakuti am'balalitse ndi kumjejemetsa. Akatero munthu uja amayamba kulimbana ndi zomwe Satana wabweretsa zija uku akuononga madera ena a moyo wake.

5. KUKHALA WOYEMBEKEZERA

Kukhala woyembekezera m'masewera omenyana ndi kofunika. Wina akakhala watcheru amatha kulingalira zomwe mdani angaganize kuchita ndi kuphelera mosavuta.

Chilichonse chomwe angachite chimakhala chosavuta kuphelera chifukwa chifukwa chokhala tcheru ndi kupenekera chomwe mdani akulingalira kuchichita.

Izi ziri chomwecho ngakhale m'moyo wauzimu. Mukadziwa machenjerero a Satana ndi kuyembekezera kuti achita chiti, mumakhala kuti mwakonzeka. Simukhala odzidzimuka ndi kujejema akayamba kumenyana nanu ndipo mumgonjetsa mosavuta.

6. KUPUSITSA

Pali luso lina lomwe omenyana masewera amaligwiritsa ntchito ndilo lompusitsa, kumunamiza kuti akufuna kuchita ichi mwa dala, koma akulingalira zochita china. Izi zimampanga mzakeyo kulephera chifukwa zimaika malo ake ofooka pa mbalambanda. Mu uzimu Satana amakhala akukupusitsani nthawi ndi nthawi ndi cholinga chakuti akufooketseni m'moyo wanu wauzimu.

M'masewera omenyana, wina amachita zinthu zofuna kungompusitsa mnzake kuti amugonjetse mosavuta. Amangopanga kenakake pongofuna kupusitsa mnzakeyo kumuika pa mbalambanda ndimkumenya malo ake ofooka mwayi ukangopezeka. Muuzimu, Satananso amapanga zinthu zomwe zimakuikani inu pa mbalambanda kuti akumenyeni mosavuta. Ndipo zikachitika sachedwa amakumenyani nthawi yomweyo. Komano, mukamamenya nkhondo yauzimu ndi Satana, mudziwe kuti iyeyo ndi amene ali kale pa mbalambanda. Popeza kuti mphamvu imene iri mwa inu ndiyopambana koposa yake. Anamenyedwa kale chibakera chomwe chinamufoola kwambiri. Chotero, mukuyenera kugwiritsa ntchito mwayi womwe Khristu anakupatsani kale pamene anakugonjetsera woipayo pa moyo wanu kuti mukhale ogonjetsa.

7. KUPONYA NDI KUPHELERA

M'kumenyana kwa kuthupi, kumafunika kuphelera nkhonya zomwe winayo akubweretsa. Chimodzimidzinsu kuuzimu. Mukachita chinthu chokomera Mulungu, Satana amaima ndi kutsekereza, kapena kuti kuphelera ndi njira zake.

8. KUSAKHAZIKIKA

M'masewero omenyana, mdani wosakhazikika amakhala woopsa. Ichi ndi chifukwa chake kumafunika kumpanikizira pansu. Muuzimu, Satana ndi mdani wosakhazikika. Amayenda-yenda "uku ndi uko" ngati mkango wobuma kufunafuna wina woti ukamlikhwire. Mukuyenera kukhala maso chifukwa cha mdani woyendayendayu.

Satananso amadziwa mphamvu ya kusakhazikika kwanu. Amafuna atakumangani kuti musakhale ochita-chita pa za Mulungu. Nchifukwa chake amayesetsa nthawi zonse kuti akupanjani ndi kukupanjani ndi zochitika muuzimu.

9. KUBWELERAMO

Kulakwitsa kuli konse kochitika m' masewero omenyana kumampatsa mdani mpata. Mu uzimonso chimodzimodzi. Mukalakwitsa muuzimu, Satana amapezerapo mwayi woti akuonongeni. Komano, mukeyenera kuphunzira kudzukanso pamene mwagwa.

Nkofunika kugwiritsa ntchito kugwa kwanu kuti mumtembenukire woipayo. Mutha kugwiritsa ntchito luso lakuthawa ndi kubwezera kuti muthe kuchita izi.

M'kumenyana kwauzimu mutha kupezeka kuti mwagwa nthawi ina yake ndi kupanjika pansu ndi mdaniyo kwa kanthawi. Koma simukuyenera kukhalabe wopanikizidwa chotero. Mulungu watipatsa njira zosiyana-siyana m' Baibulo zosandusira tsoka lathu kukhala mwayi, ngati titatsatira. Luso lakuthawa ndi kubwezera muuzimu laperekedwa monga m' mene zimakhala m' masewero omenyana kuthupi.

Moyo wa Yosefe ndi chitsanzo chabwino cha izi. Anakumana ndi tsoka logulitsidwa ngati kapolo ndi kumangidwa kuponyedwa m' ndende. Koma anasandutsa matsoka amenewa kukhala mwayi wake. Mapeto ake anamgonjetsa mdaniyo.

Pali maluso ena omwe amagwiritsidwa ntchito mu masewera omenyana monga kungwetsa mdani koma ali kumbuyo, kumkoka, ndi kukanikiza. Kodi mungathe kupeza maluso angati omwewa mu nkondo yauzimu?

10. CHOLINGA

Cholinga cha masewero omenyana kuthupi ndi kugonjetsa mdani pomgwetsa kapena kukanikizira pansu. Izi zimachitika m' modzi akagwiritsa ntchito njira zingapo molumikizana komanso kumtopetsa mdaniyo.

Satana amakhala akulimbana ndi okhulupirira nthawi ndi nthawi kuyesetsa kuti awafooketse. Akatero, amafuna kuwagwetsa pansu, kuwataya ndi kuwaika mu ukapolo wa uchimo. Cholinga chake ndi kuononga mphamvu zanu monga ochita masewero omenyana. Amakhumba atakupanga inu kugwa chafufumimba.

11. KUMWETSA ZIGOLI

Kupambana mu masewero omenyana kumachitika pamene woyang'anira waonkhetsa kuchuluka kwa zigoli zomwe ali yense ali nazo. Yemwe ali ndi zigoli zambiri ndiye amapambana.

Mdani wanu wakuuzimu, Satana, anaweruzidwa kale. Iye anagonjetsedwa ndi luso loopsa kwambiri lomwe ndi imfa ndi kuuka kwa Ambuye Yesu Khristu. Mukulimbana ndi mdani yemwe waweruzidwa kale komanso ndi wolephera pa mpikisanowu. Chifukwa cha ichi simukuyeneranso kuchita mantha ndi mphamvu kapena njira zake pamene mukulimbana naye mu nkondoyi. Simukuyeneranso kugwa ndi kupanjika mu

ukapolo wa tchimo. Mutha kuima nji molimba mtima pamene mukumenyana ndi mdani wanu mu nkondo yauzimuyi ndi kumukanizabe m'chikhulupiriro osasunthika.

12. MOMWE MUKUGANIZIRA

M'masewera omenyana amatengeranso momwe munthu akuganizira. Akatswiri a masewerowa amanena kuti zolingalira kapena zokhumba za wosewera zili m'musimu ndi zofunika kwambiri:

Chikhumbokhumbo: Kulakalaka kupambana si kokwanira. Wopikisana nawo akuyenera kutsimikizika kuti apambana. Chikhumbokhumbo chimampanga munthu kupambana mu zinthu zambiri m'moyo uno.

Kukakamira: Katswiri pa masewero omenyena amakhala wokakamira ngakhale kuti akhale akulephera koma chifukwa chokakamira amadzapambana.

Cholinga: Kupambana ndiye cholinga cha masewero. Kuti izi zitheke akuyenera kutsimikizika kuti iye ndi katswiri komanso kumpanga winayo kudziwa zimenezi.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Kodi nkhondo yodziteteza ndi yotani?

3. Kodi nkhondo yopalamula ndi yotani?

4. Kodi ndi zinthu ziti zofanana zomwe zimapezeka mu nkhondo yodziteteza komanso yopalamula?

5. Lembani mwachidule ntchito za Mzimu Woyera mu nkhondo yodziteteza ndi yopalamula.

6. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira za nkhondo yodziteteza ndi yopalamula kuchokera mu masewero omenyana kuthupi.

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto a bukhu lino)

MACHITA-CHITA A LUSO

1. Simukuyenera kudalira “akavalo” (zida zakuthupi) za anthu: Masalimo 20:7. Mulungu ali ndi akavalo “auzimu.” Ziwerengeni mu Masalimo 68:17; 104:3; Yesaya 19:1; ndi 2 Mafumu 2:11.
2. Mukuyenera kumenya nkhondo yodziteteza ndi yopalamula chifukwa Satana ndi woononga: Yohane 10:10; 1 Akorinto 10:10; Mateyu 10:28.
 - Ngati mumvera Mulungu, Iye sadzalora kuti woonganongayo alowe: Eksodo 12:23
 - Satana amakuteteza ku chionongeko cha Satana: Masalimo 17:4
 - Satana ndiye mdani amene mumalimbana naye: 1 Petro 5:8
 - Musamlekerere Satana akuononga moyo wanu: 1 Timoteo 5:14
 - Ngati mumvera Mulungu, Iye adzakhala mdani wa adani anu: Eksodo 23:22
3. Simukuyenera kugonjetsedwa ndi Satana. Werengani mavesi ali m’musiwa:
Mungathe kumthamangitsa mdani: Levitiko 26:7-8; Deuteronomu 32:30; Yoswa 23:10
Mutha kukhala ndi chigonjetso: Deuteronomu 7:21; 1 Mbiri 29:11; Masalimo 5:11; 18:29; 24:8; 91:1; Yesaya 49:19; 1 Akorinto 15:57; I John 5:4
Yehova ndiye Linga lanu: 2 Samuel 22:2; Masalimo 18:2; 31:3; 71:3; 91:2; 144:2; Yeremiya 16:19
Muli ndi ulamuliro pa mdani: Masalimo 8:6; 49:14; 72:8; 119:133; Daniel 7:27; Aefeso 1:21
Chitetezo chimachokera kwa Ambuye: Proverbs 18:10; 21:31; 29:25. Masalimo 91 ndi Salimo la chitetezo.
Mulungu amakumasulani ku kupsinjika: Masalimo 25:17; 107:6,13; 19:28
Mutha kuzindikira malingaliro a mdani: II Corinthians 10:5
Mulungu amamasula msinga za mdani: Masalimo 116:16; Aroma 8:15-21; Agalatiya 5:1.
4. Paulo akamalankhula za kumenyana nkhondo, amakhala akukamba za kulimbana ndi mdani, osati ndi Mulungu muja anachitira Yakobo. Tsimikizikani kuti pamene mukulimbana si Mulungu amene mumakhala mukugwirana-gwirana naye kuti aphwanye mzimu wodzidalira kukusinthani kuchoka ku “Yakobo” kukhala “Israel.”
5. Werenganinso Chaputala 3 cha bukhu lino ndipo mulembe ntchito za Mzimu Woyera mu nkhondo ya kudziteteza ndi kupalamula:

Utumiki Wa Mzimu Woyera

Mu Nkhondo Yodziteteza

Mu Nkhondo Yopalamula

CHAPUTALA 11

ZIDA ZOMENYERA NKHONDO YODZITETEZA

ZOLINGA

Mukamaliza phunziro lino mukwanitsa kuchita izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kufotokozera zida zanu za nkondo yodziteteza
- Kupereka vesi yomwe ikufotokozera za zida za Mulungu
- Kudziwa chida chiri chonse pa zida za Mulungu
- Kufotokozera ntchito ya zida za Mulungu chimodzi chimodzi.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi. (Aefeso 6:11)

MAU OYAMBA

Mwaphunzira kale kuti nkondo yomwe mukumenya ndi yoti simungagwiritse ntchito zida zakuthupi. Ikuyenera kumenyedwa ndi zida za Mulungu, kudziteteza ngakhale kupalamula. Mwaphunzira kale za “Dongosolo la Nkhondo ya Mulungu” mu Chaputala 9. Mwaphunziranso kuti mu dongosolo la nkondo ya Mulungu muli:

- Mau a Mulungu
- Mphamvu ndi ulamuliro zopatsidwa
- Pemphero
- Kusala kudya
- Mfungulo za Ufumu
- Dzina la Yesu

Kuonjezera pa dongosolo la nkondo ili, Baibulo limatsimikizira kuti muli ndi zida zauzimu zamphamvu. Mu chaputala chino muphunzira za zida zanu za nkondo zodzitetezera muuzimu. Mu phunziro linalo muphunzira za zida zomenyera nkondo yopalamula.

NJIRA ZODZITETEZERA

Baibulo limaphunzitsa za zinthu zomwe mungachite podziteza nokha ngati wokhulupirira:

KUGONJERA NDI KUKANIZA

Potero mverani Mulungu; koma kanizani mdierekezi, ndipo adzakuthawani inu. (Yakobo 4:7)

Muone momwe aikira zinthu mu vesili. Poyamba kugonjera, kenako kukaniza. Anthu ambiri amadumpha gawo la kugonjera kungothamangira kumkaniza Satana. Amangodabwa kuti sizikutheka. Munthu amagonjetsedwa mosavuta akamachita zinthu mosadalira Mulungu. Amene

amagonjetsa mdani ndi odzichepetsa osati odzikweza ndi odziyenereza. Mukwanitsa kumkaniza Satana ngati mungadzichepetse pamaso pa Mulungu. “Kukaniza” kumatanthauza “kuima molimba mtima ndi kutsutsa mdani mnjira iliyonse angabweretse.” Baibulo silitiphunzitsa kuti tidzinka tisaka-saka ziwanda ayi, koma kuzikaniza pamene zatifikira.

MKANIZENI SATANA MOSASUNTHIKA M’CHIKHULUPIRIRO

Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire: ameneyo mumkanize okhazikika m'chikhulupiriro, podziwa kuti zowawa zomwezo zirimkukwaniridwa pa abale anu ali m'dziko. (1 Petro 5:8-9)

Kukaniza “m’chikhulupiriro” kukutanthauza kukaniza pa ulamuliro wa Mau a Mulungu.

OSAMPATSA MPATA SATANA

Musampatse Satana danga lakuti agwirensa ntchito m’moyo wanu:

Ndipo musampatse mpata mdierekezi (Aefeso 4:27).

DZIPULUMUTSENI NOKHA KU MSAMPHA WA SATANA

Mukuyenera kudzipulumutsa nokha ku msampha wa Satana pogwiritsa ntchito njira za m’Baibulo zomenyera nkondo.

Ndipo akadzipulumutse ku msampha wa mdierekezi, m'mene anagwidwa naye, ku cifuniro cace. (2 Timoteyo 2:26).

PEWANI ZILAKOLAKO ZA THUPI

“Kupewa” kumatanthauza kudzipatula nokha ndi kukana kuchita nawo zinthu zina:

Okonedwa, ndikudandaulirani ngati alendo ndi ogonera mudzikanize zilakolako za thupi zimene zicita nkondo pa moyo; (1 Petro 2:11)

Pakuti ici ndi cifuniro ca Mulungu, ciyeretso canu, kuti mudzipatule kudama; (1 Atesalonika 4:3).

Mupewe maonekedwe onse a coipa. (1 Atesalonika 5:22).

KHALANI OLIMBA

Mwa ici mudzitengere zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoza kuima citsutsire pofika tsiku loipa, ndipo, mutacita zonse, mudzacirimika. Cifukwa cace cirimikani, mutadzimangira m'cuuno mwanu ndi coonadi, mutabvalanso capacifuwa ca cilungamo; (Aefeso 6:13-14).

Umakhala olimba kuteteza zinthu zomwe ziri zako.

KHALANI MASO KU ZOIPA, PEWANI, NDI KUVULA

Werengani Aefeso 4:17-32. “Kuvula” makhalidwe onse oipa omwe alembedwa pamenepawa ndi kumenya nkondo yodziteteza.

Musakopeke ndi makhalidwe a oipa:

Inu, tsono, okonedwa, oozizindikiratu izi, cenjerani, kuti ootengedwa ndi kulakwa kwa iwo osayeruzika, mungagwe kusiya cichazikiko canu. (2 Petro 3:17).

koma anadzudzulidwa pa kulakwa kwace mwini; buru wopanda mau, wolankhula ndi mau a munthu, analetsa kuyarukakwa mneneriyo. (2 Timoteo 2:16)

“Kupewa” kumatanthauza kutchera mbuyo. Mupeze kanthu kalikonse koipa kokhuzana ndi mdani.

KUYESA MIZIMU

Kuyesesa mizimu kumathandizira kuti munthu asasoheretsedwe.

Okonedwa, musamakhulupirira mzimu uli wonse, koma yesani mizimu ngati icokera mwa Mulungu: popeza aneneri onyenga ambiri anaturuka kulowa m'dziko lapansi. (1 Yohane 4:1)

Mukamayesesa mizimu, sindiye kuti mukukaikira utumiki wa anthuwo ayi. Ngati ali owona apambana mayesowo.

PEWANI APHUNZITSI ONYENGA

Mukalandira aphunzitsi onyenga m'nyumba mwanu, mumatenga nawo gawo m'choipa chawocho. Tetezani nyumba yanu ku machenjerero a mdani.

Munthu akadza kwa inu, wosatenga ciphunzitso ici, musamlandire iye kunyumba, ndipo musamlankhule. Pakuti iye wakumlankhula ayanjana nazo nchito zace zoipa. (2 Yohane 10:11).

TAYANI ZINTHU ZA DZIKO LAPANSI

Mukuyenera kutula pansu chichonse chomwe chingapangeni kuti musakhale msilikari wabwino wa Yesu. “Kutaya” ndi njira imodzi yodzitetezera yomwe mungachite.

zowawa pamodzi nane monga msilikari wabwino wa Kristu Yesu. Msilikari sakodwa nazo nchito wamba, kuti akakondweretse iye amene adamlemba usilikari. (2 Timoteo 2:3-4)

Cifukwa cace ifenso, popeza tizingidwa nao mtambo waukuru wotere wa mboni, titaye colemetsa ciri conse, ndi cimoli Iimangotizinga, ndipo tithamange mwacipiro makaniwo adatiikira, ndi kupenyera woyambira ndi womariza wa cikhulupiro cathu, (Ahebri 12:1)

Mwa ici, mutabvula cinyanso conse ndi cisefukiro ca coipa, landirani ndi cifatso mau ookedwa mwa inu, okhoza kupulumutsa moyo wanu. (Yakobo 1:21)

BVALANI ZIDA ZA MULUNGU

Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi. (Aefeso 6:11)

“Bvalani” akuonetsera kuti pali ntchito yoti munthu achite. Kafotokozeredwe kabwino ka zida za Mulungu kali pa Aefeso 6:10-17. Werengani ndimeyi m’Baibulo.

Paulo akulankhula nkhanu ya nkondoyi motsindika kuti kulimbanaku si kwakuthupi ndipo zida zakuthupi sizingaphule kanthu. Nkhondo zauzimu zikuyenera kumenyedwa ndi zida zauzimu. Paulo akufotokozerera zida zomwe zigwiritsidwe ntchito pa nkondo yauzimuyi.

Mwa ici mudzitengere zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoza kuima citsutsire pofika tsiku loipa, ndipo, mutacita zonse, mudzacirimika. Cifukwa cace cirimikani, mutadzimangira m'cuuno mwanu ndi coonadi, mutabvalanso capacifuwa ca cilungamo; ndipo mutadzibveka mapazi anu ndi makonzedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere; koposa zonse mutadzitengeranso cikopa ca cikhulupiriro, cimene mudzakhoza kuzima naco mibvi yonse yoyaka moto ya woipayo. Mutengenso cisoti ca cipulumutso, ndi lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu; (Aefeso 6:13-17)

Cholinga cha zida ndicho kukutandizani kuima motsutsana ndi machenjerero a mdani, Satana. Ndi udindo wanu kubvala zidazi:

Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi. (Aefeso 6:11)

Koma bvalani inu Ambuye Yesu-Kristu, ndipo musaganizire za thupi kucita zofuna zace. (Aroma 13:14)

Usiku wapita, ndi dzuwa layandikira; cifukwa cace tibvule nchito za mdima, ntibvale camuna ca kuunika. (Aroma 13:12)

Mau oti “bvalani” akutanthauza “kubvala kobvaliratu.” Zida zanu za nkondo siziri ngati unifolomu ya mpira yongovala nthawi ya mpikisano ayi. Umabvaliratu zida basi nkukhala chibvalire moyo wako wonse. Monga ngati msilikari, savula unifolomu ali ku nkondo basi nkuvalanso, inunso mukavala zida za nkondo simuvulanso kufikira kukakumana ndi Ambuye. Ngati simukhala chibvalire zida nthawi zonse, mutha kugwetsedwa nthawi ina iliyonse ndi mdierekezi. Onenesetsani kuti nthawi zonse chida chilichonse mwa zida za Mulungu chiri m’ malo mwake.

Gawo loyamba la zida za Mulungu muli zinthu zitatu zomwe mwachita kale. “Mutatha kuvala” akuonetsera chinthu chomwe inu mwachita kale ngati muli okhulupirira.

- Mutavala lamba la choonadi m’chiuno mwanu (vs 14).
- Mutavala chapachifuwa chachilungamo (vs 14).
- Mutavala nsapato za Uthenga Wabwino ku mapazi kwanu (15).

Gawo lachiwiri muli zinthu zomwe mukuyenera kuvala panopa:

- Chikopa cha chikukhulupiriro (vs. 16).
- Chisoti cha chipulumutso (vesi 17).
- Lupanga la Mzimu (17).

Mu Aefeso 6:11 Paulo akutsindika za kuvala zida zonse za Mulungu. Ena a ife timangotanganidwa ndi gawo limodzi lokha la zida za Mulungu, osalabadira za zida zinazo. Mukuyenera kuvala zida zonse. Mutha kukhala munthu wodziwa Mau (Lupanga la Mzimu) koma m'kugonjetsedwabe chifukwa chakuti mulibe chikopa cha chikhulupiriro.

Lamba

Chida choyamba kuvalidwa mwa zida za Mulungu ndi lamba wa chikhulupiriro. Kudziko, zovala zonse za msilikari zimamangiliridwa ku lamba lomwe limabweretsa pamodzi zida zonse zomwe munthu wavala. Choonadi cha Mau a Mulungu ndi lamba lauzimu lomwe zida zina zonse zimamangiliridwako. Chinthu choyamba Satana kulimbana nacho pa munthu ndi choonadi:

Mkaziyo ndipo anati kwa njoka, Zipatso za mitengo ya m'mundamu tidye. Koma zipatso za mtengo umene uti m'kati mwa munda, Mulungu anati, Musadye umenewo, musakhudze umenewo, mungadzafe. Njokayo ndipo inati kwa mkaziyo, Kufa simudzafai; (Genesesi 3:2-4).

Choonadi chikutetezana ku mabodza ndi chinyengo cha chiphunzitso zochokera kwa mdani. Choonadi ndiye tsinde la zida zonse za nkondo. Mukuyenera kukhala ndi lamba m'chiuno mwanu lomwe ndi choonadi:

Cifukwa cace cirimikani, mutadzimangira m'cuuno mwanu ndi coonadi, mutabvalanso capacifuwa ca cilungamo; (Aefeso 6:14)

Choonadi ndi chiyani?

- Yesu anati, “Ine ndine Choonadi.” - Yohane 14:6
- Mzimu Woyera ndi “Mzimu wa choonadi.” – Yohane 14:17
- Mulungu ndi choonadi – Aroma 3:4
- Mau a Mulungu ndi choonadi – Masalimo 119:151
- Uthenga Wabwino ndi choonadi – Akolose 1:5

Chapachifuwa:

Kuthupi, chapachifuwa chimatchinjiriza kumtunda kwa thupi la msilikari kumteteza ku ziwalo zofunika monga mtima, mapapo ndi zina zotero. Chapachifuwa chauzimu cha chilungamo ndiko kukutidwa ndi chilungamo cha Khristu.

Ndi kupezedwa mwa iye, wosati wakukhala naco cilungamo canga ca m'lamulo, koma cimene ca mwa cikhulupiriro ca Kristu, cilungamoco cocokera mwa Mulungu ndi cikhulupiriro; (Afilipi 3:9)

Simungadalire kuthekera kwanu. Mumayenera kudalira Khristu. Simungakumane ndi mdani popanda chitetezo cha chilungamo Khristu:

m'mau a coonadi, mu mphamvu ya Mulungu; mwa camuna ca cilungamo kulamanja ndi kulamanzere, (2 Akorinto 6:7).

Chilungamo cha Khristu chimakuteteza “ziwalo zanu zofunika” zauzimu ku nkondo za Satana ndi chisalungamo. Chikopa chapachifuwa chimayenera kumangilidwa ku lamba la choonadi.

Nsapato:

Pali mitundu yosiyana-siyana ya nsapato malingana ndi ntchito zake. Zina ndi zoyendera, ndipo zina ndi zochitira masewero. Nsapato za asilikali zimakhala zamtundu winanso. Ndi nsapato zomwe anazipanga moti ndi zomenyera nkondo. Msilikari yemwe sangathe kuyenda ali ku nkondo basi wagonjetsedwa.

“Nsapato za makonedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere” zikuonetsera kukonzeka kulowa mu nkondo yauzimu. Nsapato zauzimuzi zimateteza chifuniro chanu ku mayesero a Satana kukutsogolereni ku njira zoipa. Zimaonetsera kukhumba kwanu kuchita ntchito iriyonse yabwino ndi kufalitsa Uthenga Wabwino ku maiko onse. Nsapato zauzimu zimenezi zikupatsani kuthekera koima motsutsana ndi mdani monga momwe Paulo akutilimbikitsa kuti titero (Aefeso 6:14).

Chikopa:

Kuthupi, chikopa chimagwiritsidwa nthito kuti chipereke chitetezo ku thupi lonse la womenya nkondo. Chikopa chanu chauzimu chimatchedwa “chikopa cha chikhulupiriro.”

Pa mitundu ingapo ya chikhulupiriro yomwe yatchulidwa m’Baibulo. Pali chikhulupiriro chopulumutsa, mphatso ya chikhulupiriro ndi chikhulupiriro ngati chipatso chauzimu. Koma chikhulupiriro cha mu “chikopa cha chikhulupiriro” ndi chikhulupiriro chodzitetezera. Chikhulupiriro chimenechi ndiko kudalira Mulungu kwatunthu komwe kumateteza moyo wanu wonse. Kumatetezani ku mivi youluka yonse ya kukaikira ndi kusakhulupirira yoponyedwa ndi mdaniyo. Chikopa chachikhupiriro ichi ndikudalira Mulungu modekha ndi motsimikizika komwe kumabwezera kwa yemwe waponyayo.

Chikopa chachikhulupiriro ndikugwiritsa ntchito Mau a Mulungu nthawi zonse m’ mavuto omwe timakumana nawo m’ moyo uno. Ndi chikhulupiriro chomwe chimakupatsani kuthekera kogonjetsa mphamvu zakumidima:

Pakuti ciri conse cabadwa mwa Mulungu cililaka dziko lapansi; ndipo ici ndi cilako tililaka naco dziko lapansi, ndico cikhulupiriro cathu. (1 Yohane 5:4).

Mophatikizana ndi chikondi cha Mulungu, chikhulupiriro chimakhala cha mphamvu kwambiri:

...mutavala chapachifuwa cha chikhulupiriro ndi chikondi.... (1 Atesalonika 5:8).

Ndi chikhulupiriro chokhazikika pa choonadi:

Adzakufungatira ndi nthenga zace, Ndipo udzathawira kungsi kwa mapiko ace; Coonadi cace ndico cikopa cocinjiriza. (Masalimo 91:4)

Ndi chikhulupiriro chokhazikika pa chipulumutso:

Ndipo mwandipatsa cikopa ca cipulumutso canu: Ndipo dzanja lamanja lanu landigwiriziza, Ndipo cifatso canu candikuza ine. (Masalimo 18:35)

Popanda chikhulupiriro, mulibe choonadi. Popanda chikhulupiriro simungalandire chipulumutso. Popanda chikhulupiriro simungapititse patsogolo kufalitsidwa kwa Uthenga Wabwino wa mtendere. Popanda chikhulupiriro simupemphe chilungamo cha Khristu ndi kugwiritsa bwino ntchito lupanga la Mzimu lomwe ndi Mau a Mulungu.

Chikhulupiriro sikupenekera kapena kuyerekeza. Ndi zeni-zeni zokhazikika pa Mau a Mulungu. Mutha kuonjezera chikhulupiriro chanu pa kumvera Mau a Mulungu (Aroma 10:17), kuchita zomwe mwakhulupirira kale (Aroma 1:17) komanso kusaka Mulungu (Ahebri 12:2).

Chisoti:

Chisoti cha chipulumutso sichinthu chomwe mumavala mukapulumuka, kumbukirani kuti tikukamba nkhanu ya zida za nkondo yauzimu pano, ndipo chiyembekezo ndi chakuti mukuvala zidazi ndi kulowa mu nkondo muli kale wokhulupirira.

Chisoti cha chipulumutso chikuimirira maganizo osinthika. Chikuimirira kaganizidwe kosandulizika ndi kokonzedwanso. Muphunzira posachedwapa kuti Satana amalimbira kumalamulira maganizo athu. Ndipo izi zimapangitsa Mkhristu wa maganizo osasinthika kukhala wosavuta kugonjetsedwa ndi chinyengo chauchimo.

Paulo akulankhula za chisoti monga “chiyembekezo cha chipulumutso” mu 1 Atesalonika 5:8. Munthu akamvetsa bwino ndi kulandira chipulumutso, maganizo ake amakhala otetezeka. Chipulumutsa chimafikira ntchito za munthu za m’mbuyo, za lero, komanso za mtsogolo. Mwapulumutsidwa ku kutsutsika ndi chilango cha uchimo wanu wam’mbuyo. Mukupulumutsidwa ku mphamvu yauchimo wa lero. “Chiyembekezo cha chipulumutso” chimakamba za mtsogolo. Ndiko kupulumutsidwa komaliza ku uchimo wonse pamene Yesu adzabweranso. Chiyembekezo cha chipulumutso cha m’tsogolochi chimalimbikitsa maganizo anu kuti Satana asakuyeseni. Muli chiyembekezo chotsimikizika mtsogolo chifukwa Mulungu akumakwaniritsa zolinga zake.

Anatizindikiritse ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10).

Lupanga la Mzimu

“Lupanga la Mzimu” ndi Mau a Mulungu. Ndi chida chodzitetzera komanso chomenyera nkondo yopalamula. Mwaphunzira kale momwe Yesu anagwiritsira ntchito Mau a Mulungu ngati chida chodzitetzera. Mwaphunzira kalenso momwe Yesu anagwiritsira ntchito Mau a Mulungu polimbana ndi machenjerero a Satana. Mu phunziro lotsatirali muphunzira momwe chida chimenechi chimagwirira ntchito mu nkondo yopalamula.

Pemphero:

Atatha kufotokozerwa zida za msilikari wa Chikristu, Paulo akulankhula kuti:

mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu, ndipo poezera pamenepo cicezerere ndi kupembedzera oyera mtima onse, (Aefeso 6:18).

Monga mwaphunzira kale za “Dongosolo la Nkhondo ya Mulungu” Pemphero pamodzi ndi kusala kudya ndi zida zauzimu zamphamvu kwambiri. Zida ziwiri izi zitha kugwiritsidwa ntchito mu nkondo yodziteza komanso mu nkondo yopalamula. Onani m’musimu momwe talemba mwachidule zida za nkondo za Mulungu ndi zolinga zake:

ZIDA ZA MULUNGU

Cotsalira, tadzilimbikani mwa Ambuye, ndi m'kulimba kwa mphamvu yace. Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi. Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. Mwa ici mudzitengere zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoza kuimacitsutsire pofika tsiku loipa, ndipo, mutacita zonse, mudzacirimika. Cifukwa cace cirimikani, mutadzimangira m'cuuno mwanu ndi coonadi, mutabvalanso capacifuwa ca cilungamo; ndipo mutadzibveka mapazi anu ndi makonzedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere; koposa zonse mutadzitengeranso cikopa ca cikhulupiriro, cimene mudzakhoza kuzima naco mibvi yonse yoyaka moto ya woipayo. Mutengenso cisoti ca cipulumutso, ndi lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu; mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu, ndipo poezera pamenepo cicezerere ndi kupembedzera oyera mtima onse, (Aefeso 6:10-18)

ZIDA ZA MULUNGU

Aefeso 6:10-18

CHOONADI(lamba)



Lupanga la Mzimu

amateteza KUCHINYENGO



CHILUNGAMO(chapachifuwa)

Chimateteza ku KUSALUNGAMA



MTENDERE(nsapato)

Zimateteza ku CHISOKONEZO chazimu



CHIKHULUPIRIRO (chikopa)

Chimateteza ku KUSAKHULUPIRIRA



CHIPULUMUTSO(chisoti)

Chimateteza ku UKAPOLO

- Lamba amateteza munthu ku chinyengo cha Satana chomwe chitha kukutsogolerani ku chisalungamo (chimo).
- Chapachifuwa cha chilungamo chimakutetezani ku chisalungamo chomwe chimatsogolera ku chisokonezo.
- Nsapato za makonzedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere zimakutetezani ku chisokonezo chazimu chomwe chimatsogolera ku kusakhulupirira.
- Chikopa cha chikhulupiriro chimakutetezani ku kusakhulupirira komwe kumathera ku ukapolo. Chisoti cha chipulumutso chimateteza ku ukapolo.
- Lupanga la Mzimu, Mau a Mulungu, limagwiritsidwa ntchito podziteza komanso pomenya nkondo yodziteza.

Onani momwe munthu wosavala zida za Mulungu amakhalira wopanda chitetezo. Amagwa kuchokera ku chinyengo chotsogolera ku chisalungamo (tchimo) lomwe nthawi zonse limatsogolera ku chisokonezo. Chisokonezo chimatsogolera ku kusakhulupirira, ndipo kusakhulupirira kumathera ku ukapolo.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira za zida zauzimu zodzitetezera:

3. Perekani vesi lomwe limafotokozera za zida za Mulungu.

4. Lembani gawo lirilonse la zida za Mulungu ndikufotokozera ntchito zake:

Gawo la Chida

Ntchito

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto a bukhu lino)

MACHITA-CHITA A LUSO

1. Werengani Masalimo 45:3 ndi Yesaya 59:17. Mavesi onsewa akulankhula za Mulungu akuvala zida. Kodi ndi magawo awiri ati a zida omwe Mulungu akuvala koma sapezeka mu mndandanda wa zida zathu za nkondo zauzimu.
2. Davide akutchula za zida zauzimu pamene akukumbikira momwe Mulungu anamthandizira mu nkondo. Werengani Masalimo 18:29-50.
3. Nkofunika kudziwa bwino kagwiritsidwe ntchito ka zida za zauzimu. Werengani zomwe zidachitika pamene Davide anayesera kuvala zida zomwe sanazizolowere mu 1 Samuel 17.
4. Mulungu amagwiritsa ntchito zida zauzimu kukutetezani kwa adani anu: Masalimo 35:1-3.
Davide analankhula zambiri zolankhula zokhuza adani ake:
Werengani zomwe Mulungu amanena zokhuza adani anu:
5. Mulungu ndi chishango chanu: Onani
6. Werengani Eksodo 17. Israel anathiridwa nkondo ndipo Mulungu anamuuzira Moses kuti atase ndodo yake. M'mbuyomu, Mose anagwiritsa ntchito ndodoyi ngati ndodo ya m'busa kubweretsa madzi pakati pa anthu a Mulungu. Tsopano, kwa nthawi yoyamba, akutasa ndodo ija kuletsa maukulu ndi maulamuliro a makamamu a mizimu yoipa yauzimu ya Amaleki. Pali phunziro lalikulu mu nkhani imeneyi. Atsogoleri a nkhoa za Mulungu ali ndi udindo wogwiritsa ntchito ndodo ya Mulungu kuteteza anthu ake.
7. Kodi mumachita chiyani ku mivi ya moto yomwe mdierekezi amaiponya kwa inu? Tangoganizani za momwe mungagwiritsire ntchito chikopa cha chikhulupiro kudziteteza nokha kwa mdani. Lembani mayankho anu kuti muwagwiritse ntchito pamene Satana ayamba kulimbana nanu:
 - Kudzikonda:
 - Kusilira:
 - Kunyada:
 - Kukaikira:
 - Kufooketsedwa:
 - Kupsinjika:
 - Chilako lako choipa:
 - Umbombo:
 - Kukwiya:

CHAPUTALA 12

ZIDA ZOMENYERA NKHONDO YOPALAMULA

ZOLINGA

Mukamaliza phunziro lino muzikwanitsa kuchita izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kudziwa zida zanu zodzitetzera

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Yehova watsegula pa nyumba ya zida zace, ndipo waturutsa zida za mkwiyo wace; pakuti Ambuye Yehova wa makamu, ali ndi nchito m'dziko la Akasidi. (Yeremiya 50:25).

MAU OYAMBA

Popeza mwaphunzira tsopano momwe mungadzitetere nokha muuzimu, mukuyeneranso kuphunzira momwe mungamenyere nkondo yopalamula ndipo zikuthandizani kulimba mtima kulowa mdera la mdani. Ndi zina za nkondo yopalamula, mukwanitsa kulanda madera ena atsopano pamene mukufalitsa Uthenga Wabwino ndi kumasula anthu omangidwa mu msinga za mdani.

Kuti “mumenye nkondo yabwino” ndi zodziwikiratu kuti pafunika kukampalamula mdani:

Lamulo ili ndipereka kwa iwe, mwana wanga Timoteo, kuti, emonga mwa zonenera zidakutsogolera iwe kale, ulimbane nayo nkondo yabwino; (1 Timoteyu 1:18).

Limba nayo nkondo yabwino ya cikhulupiriro, gwira moyo wosatha, umene adakuitanira, ndipo wabvomereza cibvomerezo cabwino pamaso pa mboni zambiri. (1 Timoteyu 6:12).

Mukuyenera kumenya nkondoyi mwanzeru kwambiri ndi cholinga:

Cifukwa cace ine ndithamanga coteru, si nonga cosinkhasinkha. Ndilimbana coteru, si monga ngati kupanda nlengalenga; (1 Akorinto 9:26)

Kudziwa zida zanu zomenyera nkondo yopalamula zikupatsani kuthekera kumenya nkondo molimba mtima ndi cholinga osati mokayikira.

NJIRA ZOMENYERA NKHONDO YOPALAMULA

Izi ndi zida zomwe mungagwiritse ntchito pomenya nkhondo yopalamula:

PEMPHERO

Mwaphunzira kale za kusala kudya ndi kupemphera mu Chaputala 10 (Dongosolo la Nkhondo ya Mulungu) ndi monga chida chodzitetzera mu phunziro langopitali. Koma pemphero ndi chida champhamvu kwambiri chomenyera nkhondo yopalamula. Kukaligwiritsa ntchito kumenya nkhondo yopalamula, simmangopempherera zofuna, zosowa ndi mavuto anu okha ayi. Mmakhala mukupembedzera anthu, atsogoleri ndi maiko, kugwetsa panso malinga a Satana ndi mphamvu zake za ziwanda.

Akhristu onse akuyenera azikhala ndi nthawi yopembedzera, koma ena anayitanidwa ku utumiki wopembedzera. Utumiki wa mphamvu uwu umabweretsa wopembedzera pamaso pa Mulungu kuti amenye nkhondo zikulu-zikulu mdziko lauzimu.

Mphamvu ya matamando ndi mayamiko yatchulidwanso mu Chaputala 10. Matamando ndi mayamiko ndi zida zamphamvu kwambiri mu nkhondo yopalamula. Mu 2 Mbiri 20 pamene Israel amakumana ndi mdani, iwo anayamba kuimba nyimbo zomlemekeza Mulungu ndipo Mulungu anakantha adani onse. Mukayamba kutamanda ndi kulemekeza Ambuye, pamenepo mumakhala muku

LUPANGA LA MZIMU

Zakudya ndizo za mimba, ndi mimba ndiyo ya zakudya; koma Mulungu adzathera iyi ndi izi. Koma thupi siliri la cigololo, koma la Ambuye, ndi Ambuye wa thupi;(Aefeso 6:13).

“Kutenga” chinthu ndiko kugwira ndi kugwiritsa, kenako nkunyamula. Kutenga zida za Mulungu ndiye kuti wokhulupirira akuchitapo kanthu.

Mwaphunzira gawo la kudziteteza la zida za Mulungu mu phunziro lapitali monga lamba la choonadi, chapamtima cha chilungamo, chisoti cha chipulumutso, nsapato zokonzekera mtendere, ndi lupanga la Mzimu.

Lupanga la Mzimu lomwe ndi Mau a Mulungu, ndi chida chomwe chikhoza kugwiritsidwa pomenya nkhondo yodzitetzera ngakhalenso yopalamula. Mau amakhala chida chodzitetzera mukawagwiritsa ntchito polimbana ndi machenjejerero a Satana. Amakhala chida chomenyera nkhondo yopalamula mukawagwiritsa ntchito pofuna kutengera dera latsopano kwa Ambuye kudzera nkugawa Uthenga Wabwino ndi kumasula anthu mu msinga.

Pali mau awiri omwe osiyana omwe agwiritsidwa ntchito m’Baibulo pofotokozera za “Mau a Mulungu.” Mau oyamba ndi “logosi” omwe zonse zolankhulidwa ndi Mulungu. Apa tikukamba za bvumbulutso lonse la Mulungu kapena kuti Baibulo. Mau enawo ndi “rema.” Awa ndi mau

apaderadera a Mulungu olankhulidwa mwa bvumbulutso pa nyengo ina yake. Amenewa ndiye mau amene agwiritsidwa ntchito kutchula Mau a Mulungu lupanga la Mzimu.

Mukukumbikira Yesu anagwiritsako ntchito mau a “rema” apaderadera ogwirizana ndi yesero lomwe analimo nthawi imeneyo. Kuti izi zichitike pakufunika kudziwa bwino Mau onse a Mulungu.

Ngati mwagwiritsa ntchito mau ena ake a Mulungu pa nyengo yomwe mwakumana nayo, ndiye kuti muli ndi chidziwitso cha bvumbulutso lonse la Mulungu.

MAGANIZO A KHRISTU

Popeza Kristu adamva zowawa m'thupi, mudzikonzere mtima womwewo; pakuti iye amene adamva zowawa m'thupi walekana nalo cimo; (1 Petro 4:1)

Mukhale nao mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Kristu Yesu, (Afilipi 2:5)

“Kulola” ndiko kuvomereza kapena kugwirizana nazo. Mukuyenera kukhala nawo maganizo kapena mtima womwe unali mwa Khristu, mtima wokonzeka kumenya nkondo mwakathithi ndi mopanda mantha.

iye wocita cimo ali wocokera mwa mdierekezi, cifukwa mdierekezi amacimwa kuyambira paciyambi. Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge nchito za mdierekezi, (1 Yohane 3:8).

Mukuyenera “kulola” kuti mtima umenewu ubadwe mkati mwanu. Mukuyenera kukhala munthu wamachawi ndi wokonzeka kumenya nkondo ndi maganizo onga a Yesu.

musafanizidwe ndi makhalidwe a panso pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro. (Aroma 12:2).

Kusandulika ndiko kusinthika kwatunthu komwe kumaonekera mu chikhalidwe komanso machitidwe a munthu. Kukonzanso ndi kuvala mtima wa Khristu kumabweretsa kusandulika kotere.

KUGWETSA NDI KUPHWASULA

Cholinga cha nkondo yopalamula ndi kugwetsa ndi kuphwasula malinga a mdani:

Pakuti zida za nkondo yathu siziri za thupi, koma zamphamvu mwa Mulungu zakupasula malinga); ndi kugwetsa matsutsano, ndi cokwezeka conse cimene cidzikweza pokana ddziwitso ca Mulungu, ndi kugonjetsa ganizo lonse ku kumvera kwa Kristu; (2 Akorinto 10:4-5).

“Kugwetsa” kumatanthauza kugwetsa chinthu mwamphamvu. Kuphwasula ndiko kuchotsa ndi kutaya. Mwauzidwa kuti muphwasule ntchito za mdima (Aroma 13:12) ndi kusamusa mphamvu za ziwanda (Mateyu 10:8).

Mukamagwetsa ndi kuphwasula malinga a Satana ndiye kuti mukumenya nkhondo yopalamula. Simukhala mukudikira kuti Satana akuyambeni ayi, koma inuyo mukuyamba kuthira nkhondo malinga a mphamvu za mdani.

KUMANGA NDI KUMASULA

Muli ndi mphamvu zomanga mphamvu za kumdimba ndi kumasula mphamvu za kuunika:

Ndidzakupatsa mafungulo a Ufumu wa Kumwamba; ndipo cimene ukamanga pa dziko lapansi cidzakhala comangidwa Kumwamba: ndipo cimene ukacimasula pa dziko lapansi, cidzakhala comasulidwa Kumwamba. (Mateyu 16:19).

Ndi mphamvu komanso ulamuliro wochokera kwa Yesu, mutha kumanga ndi kumasula mphamvu zauzimu. Dziwani kuti chida ichi chimagwira ntchito ngati chimodzi: Kumanga ndi kumasula. Pamene mwamanga china chake, mukuyenera kumasula chinthu china. Mwachitsanzo, ngati mwamanga mzimu wa bodza mukuyenera kumasula mzimu wa choonadi kuti uyambe kugwira ntchito m’ malo mwake.

MWANZI WA YESU

Pamene Yesu anamwalira pa mtanda wa Kavari, anatimasula ife ku ulamuliro wa tchimo ndi mphamvu ya mdani. Mwanzi wake umatipatsa mwayi wofika pamaso pa Mulungu ndi kutimasula ku mphamvu ya Satana. Mau a Mulungu amanena kuti “iwo (okhulupirira) anamgonjetsa iye (Satana) ndi mwanzi wa Mwana wa Nkhosa (Yesu Khristu)” (Chibvumbulutso 12:11).

Chipulumutso, machiritso ndi mamasulidwe zikupezeka zonse chifukwa cha mwanzi wa Yesu. Mwanzi wake umakupatsani kuthekera komenya nkhondo yopalamula chifukwa cha miyoyo ya amuna ndi akazi ndi kubweretsa mamasulidwe ndi machiritso mu dzina la Yesu. Muli ndi mphamvu “yogonjetsa” mdani chifukwa cha “mwanzi wa Mwana wa nkhosa.”

UMBONI WANU

Chibvumbulutso 12:11 akuonetsa kuti mdani amagonjetsedwanso ndi “mau a pakamwa panu.” (umboni). Mau oti “umboni” amatanthauza kutsimikizira monga achitira mboni za kubwalo la milandu.

Mukukumbukira kuti Yesu amatha kulamulira anthu omwe amasulidwa kuti amuke nakachitira umboni kwa ena zomwe Mulungu wawachitira. Pamene muchitira umboni kapena kupereka

chitsimikizo za mphamvu ya Mulungu m'moyo wanu, mumakhala mukumenya nkondo yauzimu yopalamula pa moyo wanu. Kuti mukhale wamphamvu, umboni wanu ukuyenera ukhale wolingana ndi Mau a Mulungu, monga woimira anthu pa milandu amalankhula molinga ndi malamulo a dzikolo.

DZINA LA YESU

Mwaphunzira kale kuti dzina la Yesu ndi mbali imodzi ya dongosolo la nkondo ya Mulungu. Dzina la Yesu ndi chidanso champhamvu chomenyera nkondo yauzimu. Yesu anati, “mu dzina langa” mudzasamutsa ziwanda, kuchiritsa odwala, ndi kugonjetsa mphamvu zonse za mdani (Marko 16:17).

Onaninso maina osiyana-siyana a Yesu mu Chaputala 3 cha bukhu lino ndikuona kuti ndi maina ati omwe akugwirizana ndi kumenya nkondo yopalamula mdani. Muwerengenso bukhu la machitidwe ndipo muone zozizwitsa zomwe zinachitika “mu dzina lake.”

Dzina la Yesu sikuti ndi mau ena ake amatsenga omwe timamaliza nawo mapemphero athu. Ndi chizindikiro cha ulamuliro ndi mphamvu zopatsidwa kwa ife. Ukuyenera ukhale kuti wapatsidwa kaye mphamvu ndi ulamuliro wogwiritsa ntchito dzina la Yesu usanayambe kuligwiritsa ntchito dzinalo mu nkondo yolimbana ndi mphamvu za Satana. Onani nkhani ya pa Machitidwe 19:13-17 ndi kuona zomwe zinachitika ndi ana a Sceva.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Lembani mwachidule zomwe mwaphuzira za zida zomenyera nkhondo yopalamula:

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto a bukhu lino).

MACHITA-CHITA A LUSO

1. Werengani mavesi awa pa ntchito yopalamula ya “kusamutsa”: Mateyu 5:29-30; 7:5; 8:16; Marko 16:17; Aroma 13:12; 2 Akorinto 10:5; 1 Petro 5:7
2. Werengani mavesi awa pa ntchito yopalamula ya “kuika”: Aroma 13:12, 14; 1 Akorinto 5:13; 13:11; Agalatiya 3:27; Aefeso 4:22-24; 6:11; Akolose 3:8-14
3. Werengani mavesi awa pa ntchito yopalamula ya “kutenga”: 1 Akorinto 3:10; 8:9; 10:12; Agalatiya 5:15; Aefeso 6:13,17; 1 Timoteyo 4:16; Ahebri 3:12.
4. Monga mwaphunzira kale mu chaputala chino, mukuyenera kutenga nawo mbali mu nkondo yopalamulayi mosanyengelera kumgonjetsa mdani. Mukuyenera kuvomereza zinthu zina m’oyo wanu wauzimu kuti mupambane. Werengani mavesi ali m’oyi ndipo kumapeto kwakeko mulembe zomwe Baibulo likunena kuti mulole m’oyo wanu:

VESI

Mateyu 5:16
Yohane 4:1,27
Aroma 13:1,12-13
Aroma 14:5,13,16,19
1 Akorinto 3:18-21
1 Akorinto 10:8-9
2 Akorinto 7:1
2 Akorinto 10:17
Agalatiya 5:26
Aefeso 4:26-31
Aefeso 5:3,6,33
Afilipi 1:27
Afilipi 2:3,5
Afilipi 3:15-16
Afilipi 4:5-6
Akolose 3:15-16
Akolose 4:6
1 Atesalonika 5:6-8
2 Timoteyo 2:19
Ahebri 4:1,14,16
Ahebri 6:1
Ahebri 10:22-24
Ahebri 12:1
Ahebri 13:1,5,15

CHOMWE MULOLE

Yakobo 1:5-9
Yakobo 3:13
Yakobo 4:9
Yakobo 5:13
1 Petro 3:3-4,10-11
1 Petro 4:11,15,16,19
1 Petro 2:24
1 Yohane 3:7,18
1 Yohane 4:7

CHAPUTALA 13

ZINTHU ZA KUTHUPI ZOFANANA NDI NKHONDO YA UZIMU

ZOLINGA:

Mukamaliza phunziro lino muyenera kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kufotokozera chifukwa chomwe mau oti “nkhondo” agwiritsidwa ntchito pokamba za kulimbana kwa pakati pa mdima ndi kuunika.
- Kulemba mwachidule mfundo za kuthupi za nkhondo zomwe zingagwiritsidwe ntchito mu nkhondo yauzimu.
- Kugwiritsa ntchito mfundo za kuthupi mu dziko lauzimu.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Lamulo ili ndipereka kwa iwe, mwana wanga Timoteo, kuti, emonga mwa zonenera zidakutsogolera iwe kale, ulimbane nayo nkhondo yabwino; (1 Timoteyo 1:18).

MAU OYAMBA

Mpingo woyamba unatenga utumiki monga ngati nkhondo. Chitetezo chikufotokezedwa ngati “zida za Mulungu.” Mau a Mulungu akuyerekezedwa ndi “lupanga.” Nkhondo ya Satana ikutchedwa “mivi yoyaka moto” ndipo chikhulupiriro ndi “kulimbana kwabwino.” Okhulupirira akuuzidwa kuti “alimbane nako kulimbana kwabwino.”

Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anasankha kugwiritsa ntchito machitidwe a nkhondo yakuthupi kuti afotokozere zomwe zikuchitika mu dziko lauzimu pakati pa mdima ndi kuunika. Yankho likupezeka mu mfundo yodziwika ya Baibulo: Mfundo za kuthupi za choonadi cha uzimu. Mulungu amagwiritsa ntchito zomwe zimachitika m’oyo wa kuthupi pofotokozera zauzimu. Ife timamvetsa bwino zomwe zikuchitika kuthupi. Ndiye zauzimu zikafotokozeredwa molingana ndi za kuthupi zomwe timazidziwa kale, pamakhala posavuta kumvetsa zauzimuzo.

Yesu anagwiritsa ntchito mfundo imeneyi kwambiri. Anagwiritsa ntchito kholola la kuthupi kuti afotokozere za kholola lalikulu lauzimu lomwe amaitanirako ogwira ntchito. Pali zofanana zambiri pakati pa kholola la kuthupi ndi kholola la kuuzimu.

Izi ziri chomwecho ngakhale ku nkhondo yauzimu. Pali mfundo zambiri za nkhondo ya kuthupi zomwe zafufuzidwa ndi kugwiritsidwa ntchito ndi akadaulo mu nkhondo ya kuthupi. Mfundo zimenezi zithanso kugwiritsidwa ntchito m’dziko lauzimu. Chaputala chino chapereka mfundo za nkhondo yakuthupi zomwe zitha kugwiritsidwa ntchito mu nkhondo yauzimu. Chimabweretsa

poyera chifukwa chimene Mulungu anasankhira mfundo za nkondo ya kuthupi kuti afotokozere za nkondo yosatha yomwe okhulupirira akulimbana nayo.

ZINTHU ZA KUTHUPI ZOFANANA NDI NKONDO YAUZIMU

Izi ndi mfundo za nkondo ya kuthupi zomwe zingafanane ndi nkondo yauzimu:

TANTHAUZO LA NKONDO

Ku thupi, tanthauzo losavuta la nkondo ndi “kugwiritsa ntchito mphamvu kumpanga mdani achite zofuna zathu.” Tanthauzo ili ndilogwira ngakhale ku dziko lauzimu. Satana amakhala akugwiritsa ntchito mphamvu za ziwanda kukupangani inu kuchita ndi kukwaniritsa zofuna zake.

MOYO WA NTHAWI YA NKONDO

Dziko likakhala pa nkondo, moyo wa tsiku ndi tsiku wa anthu umakhuzidwa. Amuna amaleka ntchito zawo kuti akamenyere nkondo dziko lawo. Amatenga ma ola ambiri kukonzekera ndi kuphunzira kumenya nkondo. Ndalama zimachotsedwa ku boma kuti zigwire ntchito ku nkondo. Mzika za dzikolo zimakhala tcheru kwa adani ndipo asilikali owonjezera amaikidwa m'malire kulondera dziko.

M'dziko lauzimu, okhulupirira ambiri sakudziwa za nkondo yomwe ikumenyedwa mozungulira iwo ndipo sakukhala moyo wonga ngati wa nthawi ya nkondo. Mipingo imakonza madongosolo ndi maphwando koma alibe dongosolo la nkondo. Amakhala moyo wosangalala uku Satana akutenga miyanda miyanda ya anthu osatembenuka mtima. Anthu mu mpingo akukhala okhumudutsidwa, a nkawa komanso m'moyo wa chithupithupi. Iwo ndi akapolo a nkondo yomwe sakudziwa nkomwe kuti ilipo. Mukuyenera kumvetsa: Anthufe tili pa nkondo! Tikuyenera kukhala moyo wolingana nkuti tili mu nkondo yauzimu. Maso athu akhale tcheru pa nkondo yauzimu yomwe ikuchitika. Tizitenga nthawi kuphunzira ndi kukonzekera za nkondo. Tiphunzire za zida zathu ndi kagwiritsidwe ntchito kake.

Tigwiritse ntchito chuma chathu kupititsa patsogolo Uthenga Wabwino kuti tikapindule miyoyo yomwe ili pa chiopsezo cha Satana mdierekezi. Tikhale tcheru ku machenjerero a mdani ndi kuika asilikari owonjezera m'malire a mtima wathu, maganizo, lilime, moyo, mzimu, nyumba, dera, komanso mpingo wathu. Tili pa nkondo, ndipo moyo wathu uzionetsera zimenezi muuzimu.

CHOLINGA CHA NKONDO

Cholinga chenicheni cha nkondo kuthupi ndicho kupambana pa mdani. Ichi ndiye cholinganso chachikulu mu nkondo yauzimu. Kutu asilikari apambane kuthupi, pali zolinga zina zing'onozing'ono zimene zimayenera kukwaniritsidwa. Asilikari akuyenera agonjetse tinkhondo

ting'ono-ting'ono tamkati mwa nkondo yaikulu komanso kulanda maderana ena ndi ena. Zonsezi zimapangitsa kupambana nkondo yonse.

Chimodzi-modzinso muuzimu. Cholinga chathu chachikulu ndicho kupambana pa mdani. Komano tikuyenera kuigawa nkondo imeneyi mtimagawo ting'ono-ting'ono. Tikuyenera kudziwa zolinga zomwe Mulungu ali nazo pa ife pa nkondo yauzimuyi ku banja kwathu, ku mpingo kwathu, mdera lathu, ndi m'dziko lathu. Tikuyeneranso tizindikire dera lomwe Mulungu wapereka kwa ife patokha kuti tiligonjetse.

Msilikali aliyense mu nkondo ya kuthupi, amakhala ndi malo ake ndi zomwe akuyenera kuchita pa malo amenewo. Izi zili chomwecho muuzimu. Mukuyenera kudziwa zolinga za inu ngati munthu pa nokha zomwe zingathandizire kupambana kwa nkondo yonse. Wamkulu wa nkondo amapereka zolinga kwa asilikari. Mulungu ndiye Wamkulu wa nkondo wathu ndipo wapereka za paderadera kwa inu ngati msilikali wa Chikristu.

MAPHUNZIRO A USILIKARI

Kudziwa chabe zolinga za nkondo sikokwanira, msilikari akuyenera kulandira maphunziro a momwe angakwaniritsire zolinga zimenezi. Ku thupi m'maphunziro amenewa m'makhala za mdani, njira zake, kagwiritsidwe ntchito ka zida komanso dongosolo la nkondo.

Mdziko la uzimu, okhulupirira ambiri amalowa mu nkondo asanaphunzitsidwe bwino. Sadziwa machenjerero a mdani. Sadziwanso za zida zauzimu ndi momwe angagwiritsire ntchito komanso sazindikira za dongosolo la nkondo (Mau a Mulungu olembedwa).

Muuzimu, kutumiza msilikari ku nkondo asanaphunzitsidwe bwino ndi kuyitana tsoka. Chimodzimodzinso muuzimu. Mukuyenera kuphunzira za nkondo yauzimu kuti mupambane. Msilikari wa gulu la nkondo akayamba maphunziro, amaleka kukhala moyo wake ngati munthu wamba. Sakhalanso wotanganidwa ndi zokopa za dziko koma gulu la nkondo lomwe iye walowa.

Ife ngati asilikari a Mulungu sitikuyenera kutanganidwa ndi zolabadira za dziko lapansi kuti tikachite bwino pa nkondoyi. Siife anthu wamba pano pa dziko. Ndife ziphona za nkondo mu Ufumu wa Mulungu:

Umve zowawa pamodzi nane monga msilikari wabwino wa Kristu Yesu. Msilikari sakodwa nazo nchito wamba, kuti akakondweretse iye amene adamlemba usilikari. (2 Timoteyo 2:3-4).

KUIPITSIRANA MBIRI

Maiko omwe ali pa nkondo amakhala akunenerana zoipa komanso mabodza nthawi ndi nthawi. Satana nayenso amakhala akuikiza mabodza m'malingaliro anu mukampatsa mpata. Muphunzira zambiri za izi mu Chaputala 15 mu phunziro lotchedwa “Nkhondo M'malingaliro.”

KUFOOKETSA DZIKO MWA UKADAULO

Njira imodzi yomwe maiko omwe ali pa nkondo amagwiritsa ntchito ndi yofooketsa dziko linalo koma mwa ukadaulo. Amapereka maganizo owoneka a nzeru koma ali ofuna kufooketsa dzikolo. Muuzimu, satana amayesetsa kupanga okhulupirira kuti asakhale aukali ku tchimo. Amadziwa kuti ndi ukadaulo woterewu awafooketsa muuzimu.

KAFUKUFUKU

Maiko akakhala pa nkondo amachita kafukufuku wamkulu wa dziko linalo. Ndipo izi zimachitika mbali zonse ziwiri. Akatswiri a kafukufuku amenewa amatolera ndi kusanthula nkhani zokhuza mdani wawo. Ndipo zomwe apezazo amazipereka ku gulu la asilikari omwe akumenya nkondo.

Mu nkondo yauzimu, chidziwitso chomwe muli nacho pa mdani wanu ndi chofunika kwambiri ku chipambano chanu. Baibulo ndiye bukhu lanu la zakufukufuku lomwe limaulura nkhani zonse za mdani wanu. Pamene mukuphunzira za machenjerero a mdierekezi ndi njira za m'Baibulo zotsutsira machenjererowo, mukuyenera kupititsa zimenezi kwa asilikali omwe akumenya nkondo yauzimu. Satana amakhalanso akuphunzira zambiri za inu. Amafuna atadziwa madera a chifooko chanu kuti alunjikemo pokhuthirani nkondo.

NKHONDO YOPALAMULA NDI YODZITETEZA

Asilikari a nkondo ku dziko amagwiritsa ntchito njira zonse za nkondo – yopalamula komanso yodziteteza. Monga mwaphunzira kale, nkondo yopalamula ndi pamene mukunyamuka mwamphamvu kukalimbana ndi mdani. Ndipo nkondo yodziteteza ndi pamene mdani wafika ndipo inu mukuyenera kuteteza dera lanu.

Maphunzira kale kuti zofanana za nkondo yodziteteza ndi yopalamula ziripo muuzimu. Satana akakuthirani nkondo, mukuyenera kumenya nkondo yauzimu yodziteteza. Mukafuna kupindula miyoyo yatsopano kudzera nkulalikirira kwa Uthenga Wabwino, ndiye kuti mukumenya nkondo yopalamula. Mukutenga madera atsopano mu dzina la Ambuye Yesu Khristu.

Mkulu wa nkondo wina anauza asilikari ake kuti, “Sitikumba timayenje tobisalamo nkumadikira mdani azitiombera ayi. Tikhala tikupita chitsogolo koma mwa change.” Iye anati, “Mukakumba dzenje lobisalamo nkumaombera mdani, iye amadziwiratu malo eni eni omwe muli. Ndiye kuti mwadzikumbira manda. Tidzipita chitsogolo ndipo mdani azikhala akuombera pomwe tinali osadziwa pomwe tili tsopano.” Mkulu uyu samakhulupirira nkondo

yomangodziteteza. Iye amakonda kunena kuti ngati mdani ali wopanikizika palibenso chifukwa choti inu muziziteteza. Amakhulupirira kuti gulu lomwe likumenya nkondo yopalamula, limakhala ndi mwayi waukulu wopambana pa nkondo. Ndipo anati, “Ife timenya nkondo momwe tikudziwira ndipo tipambana.”

Mu nkondo yauzimu, munthu akamvetsa cholinga cha nkondo yathu – kugonjetsa mdani – sakhalanso wotanganidwa ndi kudziteteza. Kuti tipambane nkondo, tikuyenera tisakhale chete koma kukamthira nkondo Satana.

ZIDA

Mu nkondo iriyonse pamafunika zida. Zitha kukhala zida zosavuta monga uta ndi muvi kapena mkondo, kapena zovuta kwambiri monga mizinga ndi mabomba. Msilikari akuyenera kudziwa mtundu wa zida zomwe ziripo kuti zigwiritsidwe ntchito komanso magwiritsidwe ntchito ake. Zida zina anazipanga kuti zikhale zodzitetezera pamene zina ndi zomenyera nkondo yopalamula. Izi ziri chimodzimodzi ndi nkondo yauzimu. Ngati msilikari wa Khristu, mukuyenera kudziwa za zida zauzimu ndi magwiritsidwe ntchito ake. Monga mwaphunzira kale magawo awiri a nkondo. Yopalamula ndi yodziteteza. Kusiyana komwe kulipo ndi kwa mtundu wa zida basi. Musadzayerekeze kuyesedwa kugwiritsa ntchito zida za kuthupi kumenya nkondo yauzimu.

KUTHIRA NKHONDO MODZIDZIMUTSA

Njira ina yomwe asilikari amagwiritsa ntchito kuti apambane ndiyothira nkondo modzidzimutsa ndipo imakhala yoopsa. Wothiridwa nkondoyo amabalalika ndi kusowa mtengo wogwira chifukwa samayembekezera. Ndipo nthawi zambiri amagonjetsedwa.

Monga chigawenga, Satana amagwiritsanso ntchito njira yobisalira ndi kuthira nkondo modzidzimutsa. Amakuthirani nkondo mwadzidzidzi makamaka madera omwe inu simumayembekezera. Musaganize kuti mdani pobwera ayamba ndi machenjezo ayi. Izi sizimachitika mu nkondo yakuthupi. Sizingachitikenso mu nkondo yauzimu.

NKHONDO ZA M’MADERA OFUNIKIRA

Nkhondo iliyonse imakhala ndi madera ofunikira kwambiri. Kupambana nkondo yonse kumatengera kupambana m’madera amenewa. Mdani akatenga deralo, amakhala kuti walandanso madera ena onse ozungulira dera limenelo. Mu nkondo yauzimu mulinso nkondo ya m’madera ofunikira. Machitsanzo, mukalephera pa nkondo ya m’maganozidzi ndi lilime, kulephera kwanu kukhuzanso moyo, mzimu, ndi mtima wanu mwinanso thupi lonse.

Nkhondo yakudziko, asilikari amphamvu komanso ambiri amatumizidwa ku madera ngati amenewa. Izi zimachitikanso muuzimu. Mukuyenera kuonetsetsa kuti madera onse ofunikira a mdani mwaponyamo mizinga monga kulalikirira Uthenga Wabwino kwa anthu osatembenuka.

Nthawi zina zimachitika kuti kholola lacha dera lina lake, tikuyenera kutumizako magulu okalalikira Uthenga mwansanga.

Koma izi sizili chomwechi m'mipingo yathu lero. Azibusa ambiri angounjikana pamodzi modzi. Mipingo yamphamvu yambiri ili m'matauni mokhamokha. Madera ambiri a kumudzi alibe kuthekera komva Uthenga Wabwino ukulalikiridwa pafupi nawo popeza azibusa ambiri sanaphunzitsidwe mokwanira m'Mau a Mulungu. Madera amenewa ndi komwe Satana wamera mizu kwambiri ndipo tikuyenera kutumizako gulu lalikulu a nkhondo kukalalikira Uthenga Wabwino. Tikapindule maiko, mitima, maganizo ndi miyoyo ya amuna ndi akazi. Panopa magulu a nkhondo akutumizidwa malo olakwika.

KULUMIKIZANA

Kulumikizana ndi kofunika kwambiri ku nkhondo. Gulu la asilikari likuyenera kumalumikizana ndi wamkulu wawo kuti aziwapatsa malangizo ndi kuwalimbikitsa. Mdani amayesetsa kusokoneza kulumikizana kwao ndi cholinga chakuti awasokoneze ndi kuwagonjetsa.

Muuzimu, Satana amafuna atasokoneza kulukizana kwanu. Adzayesesa kukupanga inu kuti musapemphere ndi kuwerenga Mau a Mulungu popeza mumapezamo malangizo ndi chilimbikitso nthawi ya nkhondo. Ngati mutanganidwa ndi zinthu zina osalabadira kulumizana ndi wamkulu wanu koma muli ku nkhondo, mugonjetsedwa mosavuta. Utumiki wa Chikristu ndi njira yovomerezeka yolimbana ndi mdani. Koma mukasowekera mphamvu yauzimu, utumiki wanu sukhala wamphamvu. Mphamvu zanu pa nkhondo imeneyi zimachokera kwa Wamkulu wa nkhondo. Mukuyenera kumalandira malangizo ndi chilimbikitso nthawi zonse kuchokera kwa Iye kudzera m'pemphero ndi kuwerenga Mau ake.

ZOWOMBOLA NDI KUPHWASULA

Nkhondo ya kudziko ili ndi mitundu iwiri ya zowombera: zoyendayenda (mabwato, ndege, magalimoto) ndi zokhazikika (zida zongokhazikika ndi likulu la nkhondo). Zowombera zoyendayenda ndi zoopsa kwambiri mu nkhondo ya kuthupi popeza zimakhala zopalamulira. Zimakhala zikupita kukagonjetsa dera.

Muuzimu, Satana amada nkhawa kwambiri ndi zoombera zoyendayenda. Amafuna kuombera amuna ndi akazi omwe ndi amachawi mu nkhondo yauzimu kufuna kugonjetsa mdani. Iye amatha kulimbananso ndi zoombera zongokhazikika (okhulupirira omwe satanganidwa ndi kukapalamula nkhondo). Kumbukirani, mukakhala a machawi polimbana ndi mphamvu za kumidima, zimampanga Satana kumakusakani kwambiri. Amalimbana ndi zomwe mukuchita pokalowa mdera lake kukalanda miyoyo ya amuna ndi akazi omwe waika mu ukapolo.

KUTHIRA NKHONDO NDI KUBWEZERA

Mu nkondo ya kuthupi, mbali imodzi imathira nkondo ndipo ina imabwezera. Kubwezera ndiko kuletsa mbali inayo kuti isalowe mdera lanu ndi kulandanso dera. Satana amaletsa chirichonse chomwe mungachite polowa mdera lake. Mukafuna kuwerenga Mau kaya kupemphera kapena kuchita utumiki wina wake, amabwera ndi njira zake zoletsa chimenecho chisachitike. Mukazindikira za chimenechi, simukhala odabwa zikamachitika ndipo mumakhala okonzeka. Ku nkondo yakuthupi kuli mitundu iwiri yakuthira nkondo. Kuuzimunso chimodzimodzi.

1. Kuthira nkondo molunjika: Uku ndiko kuthira nkondo mwachindunji maso ndi maso. Mayesero a Satana ali ngati nkondo yobwera molunjika pamaso. Zimafunika kumkaniza ndipo amathawa.
2. Kutenga ulamuliro: Nkondo yakuthupi mdani amatha kutenga dera lomwe silake ndi kumalilamulira. Satana amachitanso chimodzimodzi kuika anthu mu ukapolo wauzimu. Iye amabwera ndikuphwasula malinga anu auzimu ndikuyamba kulamulira mbali imodzi ya moyo wanu. Sikuti amatengeratu koma amangoipanga kukhala yopanda mphamvu potumikira. Mutha kuthana naye pogwiritsa ntchito mphamvu za kumanga ndi kumasula komwe mwaphunzira kale. Mdani akuyenera kumangidwa ndipo dera lomwe akulamuliralo limasulidwe ku mphamvu yake.
3. Kuphwasula ndi Kutenga: Mdani akaphwasula dera mu nkondo yakuthupi, amatengeratu ndikuyamba kulilamulira. Izi zimafanana ndi kulowedwa ndi ziwanda muuzimu. Munthu wosapulumsidwa kapena wobwelera m'mbuyo amakhala pansu pa ulamuliro wa mzimu woipa womwe wamulowa. M'gonjetseni pomumanga mdaniyo ndi kumsamutsa.

KUYENDA

Kuti gulu la nkondo likhale lamphamvu, likuyenera kukhala loyendayenda. Lizikwanitsa kuyenda kufika dera lomwe likapamule nkondo. Ngati agwidwa ndi kumangidwa, amakhala opanda mphamvu.

Kuyenda ndi kofunika mu dziko lauzimu kuti mukwaniritse lamulo lakuti, “Pitani ku dziko lonse lapansi ndi kulalikira Uthenga Wabwino.” Kodi ndinu msilikari wa Mulungu yemwe wamangidwa ndi mdani kapena mukuyenda ndi kukwaniritsa lamulo lopititsa patsogolo Uthenga Wabwino?

Msilikari savala ndi kutenga zida za nkondo kuti akangokhala pansu kunyumba ayi. Akatha kukonzeka, amakalowa ku nkondo. Akhristu ambiri amatha kukonzekera bwino nkondo, koma kenako kukhalanso chete m'mipingo mwao osapita ku nkondo. Nkondo ikuchitika m'miseu ya m'mizinda yathu. Ikuchitika ku madera komwe Uthenga Wabwino sunafikire. Ngati simuyenda kukamenya nkondo ya Ambuye Yesu Khristu, simupambana ngakhale muli okonzeka kotheratu.

Msilikari sakhala katswiri wa luso la nkondo pongowerenga mabuku okamba za nkondo ayi. Luso limabwera akakhala kuti akumapita kokamenya nkondo. Kuwerenga bukhu lanu la nkondo (Baibulo) nkofunika, koma simungapambane nkondoyi pokhapokha munyamuke ndikuyamba kuchita zomwe mwawerengazo. Luso la nkondo yauzimu limabwera kudzera nkuchitachita monga momwe zimakhala ku nkondo ya kuthupi.

KUMVANA

Kumenya nkondo ndi ntchito ya gulu. Asilikari amafunika akhale omvana kuti apambane nkondo ndi kumgonjetsa mdani. Onse akuyenera akhale ogonjera mkulu wa nkondo m'modzi. Amapita limodzi ngati gulu. Sadzimenyera okha nkondo koma kumenyera dziko lawo. Okhulupirira nawonso akuyenera aphunzire kumvana pamene akumenya nkondo. M'malo momenyana wina ndi mnzake, tikuyenera kubweretsa pamodzi mphamvu zathu kulimbana ndi mdani.

Kuthupi, msilikari akavulala, amnzake amayesetsa kumpulumutsa. Gulu likamapita chitsogolo, limapita pamodzi. Sasiya ovulala m'mbuyo ayi, koma pakati pa gulu la amphamvu – ena kutsogolo ena kumbuyo kwao kufikira atachira nakhalanso amphamvu.

Koma gulu la nkondo la Mulungu limakonda kuombera iwo amene avulala. M'bale mwa Ambuye akabwera m'mbuyo nagwa, timakonda kumujeda ndi kuyamba kumupewa. Tikuyenera kupulumutsa iwo amene avulala muuzimu ndi kuwakuta ndi mphamvu zathu. Gulu la nkondo la Mulungu likuyenera kumayendera limodzi kupita chitsogolo osati kusiya ovulala m'mbuyo akudzifera okha m'mbali mwa njira ngati momwe zikukhalira lero ayi.

Sitikumenya nkondo mu dzina la ife eni ayi. Tikumenya nkondoyi mu dzina la Ambuye Yesu Khristu. Sitikudzimenyeranso nkondo tokha, koma tikumenyera dziko lathu la uzimu, Ufumu wa Mulungu.

KUMVERA

Ku nkondo yakuthupi, msilikari sachita zinthu zomwe wakonda. Amatsata malangizo a mkulu wa nkondo. Kumvera kwatunthu kumafunika. Ku nkondo kulibe chinthu chofunika kwambiri kuposa kumvera. Chimodzimidzinso kuuzimu. Ngati mukufuna kukhala womvera mu nkondo yauzimu, mukuyenera kutsata malangizo a mkulu wanu wa nkondo. Kumuyenera kumumvera kotheratu.

KULIMBIKA MTIMA

Katswiri wina wa nkondo wotchuka anati, “Ngati ukuopa kuomberedwa, wagonjetsedwa usanayambe kumenya nkondo... Mantha amapha anthu ambiri kuposa imfa.” Musamaopa kulephera mu nkondo yauzimu. Ngati mukuopa kuomberedwa ndi mdani, ndiye kuti mwagonjetsedwa musanayambe nkomwe.

Katswiriyu analankhulanso kuti, “Kulephera sikungakhalepo ngati munthu sanakuvomereze. Anthu amalephera pa nkondo m’ maganizo asanalephere pa nkondo yeniyeniyo. Palibe dziko lomwe lingagonjetsedwe ku nkondo pokhapokha anthu ake atavomereza kulephera.”

Ngati ku nkondo yakuthupi, munthu sangagonjetsedwe kuuzimu pokhapokha yekha atavomereza. Anthu amalephera pa nkondo yauzimu m’ maganizo kaye. Kanani kugonjetsedwa m’ maganizo mwanu.

KUGONJETSATSOGOLERI

Mkulu wina wa nkondo ankakhumba kugonjetsa kaye mtsogoleri wa gulu la nkondo la adani. Izi zinachitika kale muuzimu ndi Mkulu wa nkondo wathu. Kudzera mu imfa komanso kuuka kwake, Yesu anagonjetsa mphamvu za mdani. Chimaliziro cha nkondoyi chabvulumbulutsidwa kale m’ Mau a Mulungu. Koma asilikari a mdani adakali ochitachita mdziko. Yesu anagonjetsa mkulu wa nkondo wao, ife tapatsidwa ntchito yogonjetsa anyamata ake.

KUDZIPEREKA

Pokamba za kudzipereka, mkulu wina wa nkondo anati:

“Ife ndi anthu amwayi. Tikumenya nkondo! Tili ndi mwayi womenyera nkondo ndi kufera china chake. Anthu ambiri mwayi uwu sadzaupeza. Talingalirani za anthu osauka onse aja mumawadziwawa omwe sanakhale moyo kapena kufera china chake.... Ataya nthawi yawo yonse osachita kanthu, koma kudya, kugona ndi kupita ku ntchito basi...”

Ngati okhulupirira, tiri pa nkondo mu dziko lauzimu. Tili ndi mwayi womenyera nkondo ndi kufera chinachake. Sitingotaya nthawi ya moyo wathu pa kudya, kugona, ndi kupita ku ntchito ayi. Tikumenyera nkondo Ufumu womwe sudzatha. Tikumenyera nkondo Mkulu wa nkondo yemwe wagonjetsa kale mphamvu za mdani. Chigonjetso chatu ndi chotsimikizika. Tili ndi chinthu choyenera kukhalira ndi moyo, komanso kuchifera, ngati kungafunike kutero.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera.

2. Chifukwa chiyani chitsanzo cha nkondo yauzimu chagwiritsidwa ntchito pofotokozera kulimbana komwe kulipo pakati pa mphamvu za kumdima ndi mphamvu za kuunika?

3. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira mu chaputala chino za kufanana komwe kulipo pakati pa nkondo yakuthupi ndi nkondo ya kuuzimu.

- Tanthauzo la nkondo
- Moyo wa nthawi ya nkondo
- Cholinga cha nkondo
- Maphunziro a usilikari
- Kuipitsirana mbiri
- Kufooketsa dziko mwa ukadaulo
- Kafukufuku
- Nkhondo yopalamula ndi yodziteteza
- Zida
- Kuthira nkondo modzidzimutsa
- Nkhondo ya madera ofunika
- Kulumikizana
- Zoombera
- Kuthira nkondo ndi kubwezera
- Kuyenda
- Kumvana
- Kumvera
- Kulimbika mtima
- Kugonjetsa utsogoleri
- Kudzipereka

(Mayankho onse a mafunsowa ali kumapeto a bukhu lino)

MACHITACHITA A LUSO

1. Kuti muphunzire zambiri za zolinga za nkondo yauzimu, werengani Mateyu 28:18-20; Marko 16:15-18; Machitidwe 1:8; Aefeso 3:9-11 ndi Akolose 1:24-29. Pezani mayankho a mafunso awa:

a. Kodi wapereka zolinga zathu ndi ndani?

b. Kodi ndi zolinga ziti zomwe zaperekedwa kwa ku mpingo kwathu?

c. Kodi ndi zolinga ziti zomwe zapatsidwa kwa inu ngati munthu panokha?

2. Kuphunzira za zofanana za nkondo yakuthupi ndi nkondo yauzimu sikokwanira. Mukuyenera kugwiritsa ntchito zomwe mwaphunzirazi mu nkondo yanu ya tsiku ndi tsiku. Kudziwa zinthu koma osachita kanthu ndi zopanda phindu. Onaninso zomwe mwaphunzira mu chaputala chino, kenako lembani kandime kofotokozerawachidule momwe mugwiritsire ntchito zomwe mwaphunzirazi.

KUTHIRA NKHONDO DERA

KULOWA MU LA KUMENYANA NKHONDO

Kuthupi, kuthira dera nkhondo, ndi pamene asilikari athira nkhondo dera ndi cholinga cholimbana ndi mdani ndi kulanda dziko. Kupanga maphunziro ausilikari ndi kopanda tanthauzo ngati zomwe zaphunziridwazo sizigwiritsidwa ntchito. Ngakhale gulu la asilikari lomwe liri ndi zida zonse zomenyera nkhondo likhala lopanda mphamvu ngati lingoima osapita ku nkhondo. Kuti muchite bwino ku nkhondo, lowani mdera lomwe kukumenyedwa nkhondo.

CHAPUTALA 14

KULOWA DERA LA NKHONDO

KULIMBANA NDI DZIKO, THUPI, NDI SATANA

ZOLINGA

Pomaliza pa phunziro lino mukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kumasulira mau oti “machenjerero”
- Kumasulira mau oti “kutsutsa machenjerero”
- Kufotokozera machenjerero a Satana omwe amaphatikiza mphamvu zakumdima za dziko ndi dziko.
- Kuzindikira njira zauzimu zotsutsira machenjerero a Satana pogonjetsa dziko ndi thupi.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

podziwa ici, kuti umunthu wathu wakale unapacikidwa pamodzi ndi iye, kuti thupilo la ucimo likaonongedwe, kuti ife tisakhale akapolo a ucimo; pakuti iye amene anafa anamasulidwa kuucimo. (Aroma 6:6-7)

MAU OYAMBA

Mwavomera kulowa m’gulu la asilikali a Mulungu. Mwaphunzira za machenjerero a mdani ndi dera lake. Mwaphunzira za dongosolo la nkondo la Mulungu ndipo mwapatsidwa zida zomenyera nkondo yopalamula komanso yodziteza. Ndi phunziro lino mukulowa m’dera la nkondo tsopano kuti muyambe kumenya nkondo.

Chaputala chino ndi choyamba mu gawo la machaputala okamba za machenjerero a Satana ndi njira zomwe Baibulo likukamba zotsutsira machenjerero ake onyenga. Machenjerero ndi ukadaulo wokonza ndi kukwaniritsa njira zomenyera nkondo. Ndi dongosolo la chipambano.

MACHENJERERO A SATANA

Satana wakonza madongosolo omuthandiza kuti apambane nkondo yolimbana ndi okhulupirira. Izi ndi zimene Paulo akutanthauza akamanena za machenjerero a mdierekezi.

Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi. (Aefeso 6:11)

Mau oti “machenjerero” amatanthauza dongosolo la luso. Machenjerero a Satana ndi dongosolo lake la luso komanso lonyenga polimbana ndi okhulupirira.

NJIRA ZA MULUNGU ZOTSUTSIRA MACHENJERERO

Okhulupirira sanasiyidwe opanda chitetezo pamene mdani akuthira nkondo. Mau a Mulungu ndi bukhu la njira zomenjera nkondo yauzimu:

**kuti asaticenierere Satana; pakuti sitikhala osadziwa macenjerero ace.
(2 Akorinto 2:11)**

Mau oti machenjerero mu vesi ili akutanthauza malingiliro kapena zolinga. Baibulo liri ndi njira zotsutsira zogonjetsera mphamvu zonse za mdani.

Mau oti **kutsutsa** amatanthauza “kuchita motsutsana, kutsekereza, kugonjetsa kapena kugwetsa mphwayi.” Mu dziko lauzimu, njira yotsutsira ndi dongosolo lokonzedwa bwino lolimbana ndi Satana. Limakonzedwa kuti likatsekereze, kugonjetsa ndi kugwetsa mphwayi machenjerero a Satana.

Machaputala angapo otsatirawa akukamba za machenjerero ndi njira zotsutsira machenjererowo. Machenjerero a Satana mu dera lina lake la nkondo yauzimu afotokozeredwa kaye mu chaputala chirichonse. Kenaka, njira zapaderadera zotsutsira machenjererowo zaperekedwa kuti mukhale ogonjetsa. Mu phunziro lino muphunzira momwe dziko ndi thupi zimagwirira ntchito limodzi mu nkondo yauzimu ndi njira zotsutsira kuti tikagonjetse mphamvu zakumdima.

MACHENJERERO A SATANA: DZIKO NDI THUPI

Mwaphunzira kale mu chaputala 7 kuti dziko ndi thupi ndi madera a mdani:

SATANA AMAGWIRA NTCHITO KUDZERA MU DZIKO

Satana ndi mfumu ya dziko lapansi ndipo ngati mfumu amapangira zochita maboma ndi maiko. Amatchedwa “wonyenga maiko” mu Chibvumbulutso 20:3 ndi 7. Daniel 10 akukamba za mphamvu ya ziwanda pa dziko la Perezi yoletsa pemphero la Daniel. Satana ali ngati mkango wobuma pa dziko lapansi:

Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire: (1Petro 5:8).

Mau oti “mkango wobuma” akupereka chithunzithunzi cha njira zoopsa zomwe Satana amagwiritsa ntchito. Koma Satana amafotokozeredwanso ngati “m’ngelo wa kuunika”:

Ndipo kulibe kudabwa; pakuti Satana yemwe adzionetsa ngati mngelo wa kuunika. Cifukwa cace sikuli kanthu kwakukuru ngatinso atumiki ace adzionetsa monga

atumiki a cilungamo; amene cimariziro cao cidzakhala monga nchito zao. (2 Akorinto 11:14-15).

Ndime iyi ikufotokozera Satana ngati wokopa mochititsa chidwi, mochenjera komanso mwachinsinsi pomenya nkondo. Chotero, Satana amagwira ntchito moonekera komanso mwachinsinsi.

Machitachita a Satana pa dziko lapansi ndi osiyana-siyana, koma onsewo amakhala akulimbana ndi Mulungu, dongosolo lake komanso anthu ake. Iye amatsutsa ntchito ya Mulungu m'dziko. Izi zaonekera mu kuukira komanso kugwa kwake kuchoka kumwamba zomwe mwaphunzira kale (Ezekiel 28:12-29). Satana amatsutsana ndi ntchito ya Mulungu m'dziko. Iye ali kumbuyo kwa “mzimu wokana Khristu” pa dziko lapansi:

Pakuti onyenga ambiri adaturuka kulowa m'dziko lapansi, ndiwo amene sabvomereza kuti Yesu Kristu anadza m'thupi, Ameneyo ndiye wonyenga ndi wokana Kristu. (2 Yohane 7)

Satana amatsutsanso ntchito ya Mzimu Woyera pa dziko lapansi. Imodzi mwa ntchito za Mzimu Woyera ndi kutsogolera amuna ndi akazi ku choonadi cha Mau a Mulungu. Satana amayesetsa kuletsa Mau a Mulungu kuti asagwire ntchito m'miyoyo ya anthu:

mwa amene mulungu wa nthawi yino ya pansu pano unacititsa khungu maganizo ao a osakhulupirira, kuti ciwalitsiro ca Uthenga Wabwino wa ulemerero wa Kristu, amene ali cithunzithunzi ca Mulungu, cisawawalire. (2 Akorinto 4:4).

Satana amazunza ndi kuyesa okhulupirira pa dziko lapansi:

Mwa ici inenso, posalekereranso, ndinatuma kukazindikira cikhulupiriro canu, kuti kaperta: woyesa akadakuyesani, ndipo cibvuto cathu cikadakhala copanda pace. (1 Atesalonika 3:5).

Nati Yehova kwa Satana, Taona, zonse ali nazo zikhale m'dzanja mwako; pa iye pokha usatambasula dzanja lako. Naturuka Satana pamaso pa Yehova. (Yobu 1:12).

Satana amanyenga dziko lapansi kudzera mu “malo okwera a zoipa zauzimu.” Umu ndi m'mene amagwirira ntchito kudzera mu madongosolo a chipembedzo. Amanyenga kudzera mu zipembedzo zabodza, aphunzitsi onama, komanso ziphunzitso zonyenga.

Satana amalimbananso ndi okhulupirira omwe ali m'dziko lapansi koma sali a dziko lapansi. Mutha kuwerenga za nkondo iyi mu Aefeso 6:10-18. Satana amatsutsa ndi kuneneza abale:

Ndipo cinaponyedwa pansi cinjoka cacikuru, njoka yokalambayo, iye wochedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse; cinaponyedwa pansi kudziko, ndi angelo ace anaponyedwa naye pamodzi. Ndipo ndinamva mau akuru m'Mwamba, nanena, Tsopano zafika cipulumutso, ndi mphamvu, ndi ufumu za Mulungu wathu, ndi ulamuliro wa Kristu wace; pakuti wagwetsedwa wonenera wa abale athu, wakuwanenera pamaso pa Mulungu wathu usana ndi usiku. (Chibvumbulutso 12:9-10).

Amaika mbeu yokaikira m'maganizo a okhulupirira. Ili linali gawo limodzi la mayesero a munthu m'munda wa Eden (onani Genesisi 3:1-5).

Satana amapangitsa maiko kuti azunze okhulupirira:

zimene uti udzamve kuwawa; taona, mdierekezi adzaponya ena ainu m'nyumba yandende, kuti mukayesedwe; ndipo mudzakhala naco cisautso masiku khumi. Khala wokholupirfka kufikira imfa, ndipo ndidzakupatsa iwe korona wa moyo. (Chibvumbulutso 2:10).

Satana amayesera kutchinga okhulupirira kuti asatumikire Mulungu mwamphamvu:

cifukwa tinafuna kudza kwa inu, inedi Paulo ndatero kamodzi kapena kawiri; koma Satana anatiletsa. (1 Atesalonika 2:18).

Satana amagwiritsa ntchito kukopa kwa dziko lapansi kuti anyenge okhulupirira kuwachimwitsa. Amakopa kudzera mu zinthu zachikoka zomwe ziri pafupi nanu. Amalimbikitsa chikondi cha dziko lapansi mkati mwanu:

Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko apansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, cikondi ca Atate Isiciri mwa iye. Pakuti ciri conse ca m'dziko lapansi, cilakolakoca thupi ndi cilakolako ca maso, matamandidwe a moyo, sizicokera kwa Atate, koma ku dziko lapansi. (1 Yohane 2:15-16)

Satana amalimbananso ndi maganizo, lilime, mzimu, thupi, ndi malinga a okhulupirira. Amadzera kwa abale ndi abwenzi, mavuto a zachuma, ndi zochitika pa moyo wa munthu. Muphonzira zambiri za magawo amenewa mu machaputala ena.

Maina a Satana amauluranso za machenjerero ake pa dziko lapansi. Munaphonzira za maina a Satana mu Chaputala 5 cha phunziro lino. Werenganinso za maina a Satana ndi kuona momwe zikuonetsera machenjerero ake mdziko lero.

SATANA AMAGWIRA NTCHITO KUDZERA M'THUPI

Thupi moyo ndi mzimu wa munthu zimagwira ntchito limodzi. Satana amagwiritsa ntchito moyo ndi thupi kudzera m'thupi. Njira iyi inaonekeranso mu yesero loyamba la munthu. Hava ANAONA chipatso ndipo chinali chapwino kudya (KULAWA), ndipo chinali chokoma mmaso. Ndipo mtengo unali WOSILIRIKA kupatsa munthu nzeru" anatenga nampatsako mwamuna wake (Genesisi 3:6). Satana amagwiritsa ntchito zilakolako za thupi kuti alowe m'moyo ndi mzimu wa Hava.

Ngati Satana satsekereza malingaliro anu, ndi kukupangani kukana Uthenga Wabwino kufikira kutembenuka mtima, ndiye kuti agwiritsa ntchito thupi lanu kulimbana nanu. Zilakolako za thupi zimalimbana ndi moyo wanu:

Okonedwa, ndikudandaulirani ngati alendo ndi ogonera mudzikanize zilakolako za thupi zimene zicita nkondo pa moyo; (1 Petro 2:11).

Satana amagwiritsa ntchito thupi kuti asokoneze maganizo:

koma ndiona lamulo lina m'ziwalo zanga, lirikulimbana ndi lamulo la mtima wanga, ndi kundigonjetsa kapolo wa lamulo la m'ziwalo zanga. (Aroma 7:23)

“Ziwalo zanga” akutanthauza thupi. Satana amagwiritsa ntchito thupi kuti asokoneze mzimu:

Pokhala nao tsono malonjezano amenewa, okonedwa, tidzikonzere tokha kuleka codetsa conse ca thupi ndi ca mzimu, ndi kutsirfza ciyero m'kuopa Mulungu. (2 Akorinto 7:1).

Satana amagwiritsa ntchito thupi kukupangitsa kuti mukolole chibvuni m'moyo wanu:

Pakuti wakufesera kwa thupi la iye yekha, cocokera m'thupi adzatuta cibvundi; koma wakufesera kwa Mzimu, cocokera mu Mzimu adzatuta moyo wosatha.(Agalatiya 6:8).

Pa Aefeso 4 pamene Paulo akukamba za machimo a thupi pogwiritsa ntchito mau oti “munthu wakale ndi munthu watsopano” akupereka chenjezo ili:

Musampatse mpata mdierekezi (Aefeso 4:27).

Chenjezo ili likuonetsa kuti munthu akachita machimo a kuthupiwa, amakhala kuti wapereka mpata, malo kapena ulamuliro kwa Satana pa moyo wake. Ndipo akapitiriza kukhalabe m'moyo umenewu mwadala, amadzilowetsa mu ukapolo kwa Satana:

akadzipulumutse ku msampha wa mdierekezi, m'mene anagwidwa naye, ku cifuniro cace. (2 Timoteo 2:26).

SATANA AMAGWIRA NTCHITO KUDZERA MU ZIWANDA:

Monga muphunzire mtsogolomu, munthu wotembenuka mtima “sangadzadzidwe” ndi Satana ngati apirizabe kukhala wokhulupirira weni weni. Kudzadzidwa ndi Satana zimatanthauza ulamuliro pa thupi, moyo, ndi mzimu komanso maganizo. Koma ngati wokhulupirirayo apiriza kukhala moyo wa uchimo imafika nthawi yakuti amalowedwa ziwanda.

MOMWE ZIMAGWILIRA NTCHITO LIMODZI

Dziko, thupi, ndi mdierekezi pamodzi ndi ziwanda zake amaphatikizana polimbana ndi wokhulupirira. Mphamvu iliyonse imatha kugwira ntchito payokha, koma nthawi zambiri amalimbana ndi wokhulupirira mophatikizana. Satana amagwiritsa ntchito dziko ndi zokopa zake kuti alamulire thupi. Amagwiritsa ntchito kuti alamulire moyo, maganizo ndi mzimu. Kenaka amayesera kukupangani kuti mufanane ndi dziko osati Mulungu.

NJIRA ZAUZIMU ZOTSUTSIRA MACHENJERERO: KUGONJETA THUPI

Dziko, thupi ndi mdierekezi zimaonetsa kuti ndi zovuta kulimbana nazo. Komano nawa mavesi a mphamvu omwe muwagwiritse ntchito polimbana ndi mphamvu za woipayo:

PEREKANI THUPI LANU MONGA NSEMBE:

Munthu akalowa mu gulu la asilikali a dziko, amakhala pansu pa ulamuliro wa akuluakulu ake. Amampatsa malamulo a momwe angakhalire payekha, mavalidwe komanso mamenyedwe a nkondo. Kutu mupambane mu nkondo yauzimuyi, kumvera kotereku kukufunika:

Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansu pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro. (Aroma 12:1-2).

Mukuyenera kudzipereka nokha kwa Mulungu mwakufuna kwanu. Mu chipangano chakale, munthu akapereka nsembe, samakhalanso ndi ulamuliro pa nsembeyo. Imakhala kuti yaperekedwa kwatunthu kwa Ambuye. M'malo mofanana ndi dziko komanso thupi, mukuyenera “kusinthika” mwakusandulika kwa mtima. Muphunzira zambiri za nkondo ya m'maganizo mu Chaputala 15.

ZIVEKENI NOKHA NDI MAGANIZO A KHRISTU:

Kusandulika maganizo kumachitika pamene mukuziveka nokha ndi maganizo ofanana ndi a Yesu:

Popeza Kristu adamva zowawa m'thupi, mudzikonzere mtima womwewo; pakuti iye amene adamva zowawa m'thupi walekana nalo cimo; kuti nthawi

yotsalira simukakhalenso ndi moyo m'thupi kutsata zilakolako za anthu, koma cifuniro ca Mulungu. (1 Petro 4:1-2).

KHALANI NDI MAGANIZO OYENERA PA THUPI LANU:

Timauzidwa kuti tidane ndi “chovala chopakidwa ndi zilakolako” (Yuda 23). Mukuyenera kuzindikira kuti zilakolako za thupi siziri za Atate koma za mdierekezi:

Pakuti ciri conse ca m'dziko lapansi, cilakolakoca thupi ndi cilakolako ca maso, matamandidwe a moyo, sizicokera kwa Atate, koma ku dziko lapansi. (1 Yohane 2:16)

Musalidalire thupi:

pakuti ife ndife mdulidwe, akutumikira popembedza ndi Mzimu wa Mulungu, nadzitamandira mwa Yesu Kristu, osakhulupirira m'thupi; (Afilipi 3:3).

Mukuyenera kuzindikira kuti moyo wa thupi, umabweretsa chibvundi koma moyo wauzimu umabweretsa moyo:

Pakuti wakufesera kwa thupi la iye yekha, cocokera m'thupi adzatuta cibvundi; koma wakufesera kwa Mzimu, cocokera mu Mzimu adzatuta moyo wosatha. (Agalatiya 6:8)

DZIWANI KUTI SIMUKUYENERA KUKHALA KAPOLO WA THUPI:

Kale, muli ochimwa, munali kapolo wa thupi:

amene ife tonsenso tinagonera pakati pao kale, m'zilakolako za thupi lathu, ndi kucita zifuniro za thupi, ndi za maganizo, ndipo tinali ana a mkwiyo cibadwire, monganso otsalawo; (Aefeso 2:3)

Pakuti pamene tinali m'thupi, zilakolako za macimo, zimene zinali mwa cilamulo, zinalikucita m'ziwalo zathu, kuti zibalire imfa zipatso, Koma tsopano tinamasulidwa kucilamulo, popeza tinafa kwa ici cimene tinagwidwa naco kale; coteru kuti titumikire mu mzimu watsopano, si m'cilembo cakale ai. (Aroma 7:5-6).

Werengani Aefeso 2 ndi Aroma 8. Ndipo muona kuti simukuyeneranso kukhala pa ukapolo wa thupi. Ufulu wanu umabwera kudzera mwa Khristu:

Koma tsopano tinamasulidwa kucilamulo, popeza tinafa kwa ici cimene tinagwidwa naco kale; coteru kuti titumikire mu mzimu watsopano, si m'cilembo cakale ai. (Aroma 8:2)

PHUNZITSANI THUPI LANU KUKHALA LOMVERA

Kuthupi, msilikali ayenera kukhala womvera malamulo onse. Amaphunzira malamulo a kunkhondo akamalowa usilikali. Amapatsidwa mwayi wochita zomwe waphuzira. Akalephera amayeseranso mpaka atadziwa.

Izi zili chomwecho kuuzimu. Mukuyenera kuphunzitsa thupi lanu kumvera. Phunzirani malamulo a Mulungu. Mulungu amakupatsani mayeso pa zomwe mwaphunzira kudzera mu zokhoma zomwe moyo wanu umakumana nazo:

Okonedwa, musazizwe ndi mayesedwe amoto adakugwerani inu akhale cakukuyesani, ngati cinthu cacilendo cacitika nanu: (1 Petro 4:12)

Nati Yehova kwa Satana, Taona, zonse ali nazo zikhale m'dzanja mwako; pa iye pokha usatambasula dzanja lako. Naturuka Satana pamaso pa Yehova. (Yobu 1:12).

Kuthupi, msilikali amaphunzira kuvomera koyenera ndi kosayenera kudzera mkuyesera. Inunso mutha kuphunzira kudzera m'buku la malamulo a nkondo la Mulungu, Baibulo. Pamene mukuphuzitsa thupi lanu kumvera, muphunzira kusiyantsa chabwino ndi choipa.

Pakuti yense wakudya mkaka alibe cizolowezi ca mau a cilungamo; pakuti ali khanda. Koma cakudya cotafuna ciri ca anthu akulu misinkhu, amene mwa kucita nazo anazoloweretsa zizindikiritso zao kusiyantsa cabwino ndi coipa. (Ahebri 5:13-14).

Phunzitsani thupi lanu kumvera Mau a Mulungu. Simugonjetsa zilakolako za thupi pozikwaniritsa. Pamene Mulungu akuvumbulutsa magawo a thupi pa moyo wanu, mukuyenera kuchitapo kanthu:

Pewani zilakolako za thupi, zolimbana ndi moyo (1 Petro 2 11).

Pokhala nao tsono malonjezano amenewa, okonedwa, tidzikonzere tokha kuleka codetsa conse ca thupi ndi ca mzimu, ndi kutsirfza ciyero m'kuopa Mulungu. (2 Akorinto 7:1)

Koma bvalani inu Ambuye Yesu-Kristu, ndipo musaganizire za thupi kucita zofuna zace. (Aroma 13:14)

Onesetsani kuti mwachitapo kanthu. Mwapewa zilakolako za thupi. Mwadziyeretsa ku chidetso cha thupi komanso musakwaniritse zofuna za thupi.

VULANI MUNTHU WAKALEYO

“Munthu wakale” akuimirira thupi la uchimo. Paulo akuti:

kuti mubvule, kunena za makhalidwe anu oyamba, munthu wakale, wobvunda potsata zilakolako za cinyengo; koma kuti 1 mukonzeke, mukhale atsopano mu mzimu wa mtima wanu, 2 nimubvale munthu watsopano, amene analengedwa monga mwa Mulungu, m'cilungamo, ndi m'ciyero ca coonadi. (Aefeso 4:22-24)

FETSANI (IPHANI) THUPI LANU

Thupi lanu likuyenera kupachikidwa. Silifa imfa wamba. Mukuyenera kulipachika pokana kuti likulamulireni.

Podziwa ici, kuti umunthu wathu wakale unapacikidwa pamodzi ndi iye, kuti thupilo la ucimo likaonongedwe, kuti ife tisakhale akapolo a ucimo; pakuti iye amene anafa anamasulidwa kuucimo. (Aroma 6:6-7).

Ndinapacikidwa ndi Kristu; koma ndiri ndi mayo; wosatinso ine ai, koma Kristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndiri nao: tsopano m'thupi, ndiri nao m'cikhulupiro ca Mwana wa Mulungu, amene anandikonda, nadzipereka yekha cifukwa ca ine. (Agalatiya 2:20)

Koma iwo a Kristu Yesu adapacika thupi, ndi zokhumba zace, ndi zilakolako zace. (Agalatiya 5:24)

YENDANI MUUZIMU

Moyo wanu (m'mene mumakhalira) utha kumalamuliridwa ndi Satana kudzera m'thupi lanu, dziko kapena mphamvu ya ziwanda ngati mutazilola. Simukuyenera kulamuliridwa ndi dziko, thupi kapenanso mdierekezi ayi. Mutha kuphunzira kuyenda muuzimu:

Koma ndinena, Muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse cilakolako ca thupi. (Agalatiya 5:16)

Ngati tiri ndi moyo ndi Mzimu, ndi Mzimunso tiyende. (Agalatiya 5:25)

Kuyenda muuzimu ndiko kulola Mzimu Woyera kuti alamulire makhalidwe ndi moyo wanu. Thupi si lamphamvu kwambiri kuposa mzimu wanu. Mukalola Mzimu Woyera aonetsere mphamvu yake mwa inu, Iye adzapereka moyo ku thupi lanu.

Simukuyenera kukhala mu imfa ya uchimo. Mulungu atha kupereka moyo ku mzimu wanu kuti mukhale ndi moyo watsopano:

Ndipo ngati Kristu akhala mwa inu, thupilo ndithu liri lakufa cifukwa ca ucimo; koma mzimu uli wamoyo cifukwa ca cilungamo. Koma ngati Mzimu wa iye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, iye amene adaukitsa Kristu Yesu kwa

akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa Mzimu wace wakukhala mwa inu. Cifukwa cace, abale, ife tiri amangawa si ace a thupi ai, kukhala ndi moyo monga mwa thupi; pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi, mudzafa; koma ngati ndi mzimu mufetsa zocita zace za thupi, mudzakhala ndi moyo. Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu, (Aroma 8:10-14).

Kuti mutsogozedwe ndi Mzimu Woyera, Iye akuyenera kumakhala mwa inu. Mukuyenera kubwadwanso mwatsopano mwa Mzimu:

Cobadwa m'thupi cikhala thupi, ndipo cobadwa mwa Mzimu, cikhala mzimu. Usadabwe cifukwa ndinati kwa iwe, Uyenera kubadwa mwatsopano. (Yohane 3:6-7)

Mukuyeneranso kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Ndi Mzimu Woyera amene amakupatsani inu mphamvu kuti muyende monga mwa mzimu osati thupi. Pali phunziro mu Harvestime International Institute lokamba za utumiki wa Mzimu Woyera m'moyo wa wokhulupirira. Utumiki wa Mzimu Woyera ndi wofunika kwambiri kuti mukagonjetse dziko, thupi ndi mdierekezi. Mwa Mzimu Woyera mutha kuyenda monga mwa mzimu osati thupi.

LOLANI MZIMU WANU AZILANKHULA MWA MZIMU WOYERA:

Mulungu amalankhula ndi mzimu wanu kudzera mwa Mzimu Woyera:

Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu, (Aroma 8:14)

Mzimu Woyera athanso kulumikizana ndi Mulungu kuchokera mu mzimu wanu:

Pakuti iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu, koma ndi Mulungu; pakuti palibemunthu akumva; koma mumzimu alankhula zinsinsi. (1 Akorinto 14:2)

Mukamalankhula ndi malilime achilendo, womwe ndi umboni wogwirika wa kubatizidwa ndi Mzimu Woyera (Machitidwe 2), mzimu wanu umakhala ukulumikizana ndi Mulungu. Izi zikachitika, Mzimu Woyera amayamba kupemphera molingana ndi chifuniro cha Mulungu mwa inu:

Ndipo momwemonso Mzimu ahandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwiniatipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka; ndipo iye amene asanthula m'mitima adziwa cimene acisamalira Mzimu, cifukwa apempherera oyera mtima monga mwa cifuno ca Mulungu. (Aroma 8:26-27)

BALANI CHIPATSO CHA MZIMU

Motsutsana ndi ntchito za thupi, balani chipatso cha Mzimu Woyera. Izi ndi:

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupirtro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. (Agalatiya 5:22-23)

Chipatso cha Mzimu chafotokozeredwa bwino mu phuniziro lotchedwa “Utumiki wa Mzimu Woyera.”

MUSAKHALE NKUTSUTSIKA

Satana amatengerapo mwayi kufooka kwa thupi kukupangani kuti muzikhala otsutsika nthawi ndi nthawi. Koma Paulo anati:

Cifukwa cace tsopano iwo akukhala mwa Kristu Yesu alibe kutsutsidwa. (Aroma 8:1)

Mukalephera kukana zofuna za thupi, musakhazikike nkutsutsika. Lapani ndi kupempha chikhululukiro:

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutsambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:9)

NJIRA ZOTSUTSIRA MACHENJERERO A SATANA KUGONJETA DZIKO

Umu ndi momwe mungagonjetsere dziko.

KHALANI NDI MAGANIZO OYENERA PA DZIKO

Dziwani kuti simuli a dziko lapansi:

Ine ndawapatsa iwo mau anu; ndipo dziko lapansi linadana nao, cifukwa sakhala a dziko lapansi, monga Ine sindikhala wa dziko lapansi. Sindipempha kuti muwacotse iwo m'dziko lapansi, koma kuti muwasunge iwo kuletsa woipayo. Siali adziko lapansi monga Ine sindiri wa dziko lapansi. (Yohane 17:14-16)

Ngati dziko lapansi lida inu, mudziwa kuti lidada Ine lisanayambe kuda inu. Mukadakhala a dziko lapansi, dziko lapansi likadakonda zace za lokha; koma popeza simuli a dziko lapansi, koma Ine ndinakusankhani inu mwa dziko lapansi, cifukwa ca ici likudani inu. (Yohane 15:18-19)

Zindikirani kuti mukumana ndi chizunzo pa dziko lapansi:

Zinthu izi ndalankhula ndi inu, kuti mwa Ine mukakhale nao mtendere. M'dziko lapansi mudzakhala naco cibvuto, koma limbikani mtima; ndalilaka dziko lapansi Ine. (Yohane 16:33).

Dziwani kuti simupindula kanthu kukhala ndi zonse zapadziko ndi kutaya moyo wanu:

Pakuti munthu apindulanji akadzilemezera dziko lonse, natayapo moyo wace? (Marko 8:36)

Pakuti munthu apindulanji, akadzilemezera dziko lonse lapansi nadzitayapo, kapena kulipapo moyo wace? (Luka 9:25)

Zindikirani kuti ngati mukonda dziko lapansi mukhala mdani wa Mulungu:

Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko apansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, cikondi ca Atate Isiciri mwa iye. Pakuti ciri conse ca m'dziko lapansi, cilakolakoca thupi ndi cilakolako ca maso, matamandidwe a moyo, sizicokera kwa Atate, koma ku dziko lapansi. (1 Yohane 2:15-16)

Akazi acigololo inu, kodi simudziwa kuti ubwenzi wa dziko lapansi uti udani ndi Mulungu? Poto, iye amene afuna kukhala bwenzi la dziko lapansi adziika mdani wa Mulungu. (Yakobo 4:4)

Dziwani kuti dziko lapansi ndi kanthawi:

Ndipo dziko lapansi lipita, ndi cilakolako cace; koma iye amene acita cifuniro ca Mulungu akhala ku nthawi yonse. (1 Yohane 2:17)

ndi iwo akucita nalo dziko lapansi, monga ngati osacititsa; pakuti maonekedwe a dziko ili apita. (1 Akorinto 7:31)

Popezaizi zonse zidzakanganuka kotero, muyenera inu kukhala anthu otani nanga, m'mayendedwe opatulika ndi m'cipembedzo, (2 Petro 3:11)

DZIWANI KUTI SIMULI MU UKAPOLO WA DZIKO

Ngati wokhulupirira, simukuyenera kukhala kapolo wa machitachita a dziko. Ngakhale munali pansu pa ulamuliro wa dziko (Aefeso 2:2), panopa sindinunso kapolo:

zimene munayendamo kale, monga mwa mayendedwe a dziko lapansi lino, monga mwa mkulu wa ulamuliro wa mlengalenga, wa mzimu wakucita tsopano mwa ana a kusamvera; amene ife tonsenso tinagonera pakati pao kale, m'zilakolako za thupi

lathu, ndi kucita zifuniro za thupi, ndi za maganizo, ndipo tinali ana a mkwiyo cibadwire, monganso otsalawo; Koma tsopano mwa Yesu Kristu inu amene munali kutali kale, anakusendezeni mukhale pafupi m'mwazi wa Kristu. Pamenepo ndipo simulinsu alendo ndi ogonera, komatu muli a mudzi womwewo wa oyera mtima ndi a banja la Mulungu; (Aefeso 2:2-3, 13, 19).

Aroma 12:1-3 amaphunzitsa kuti musafanizidwe ndi maonekedwe a dziko lapansi. Mutha kusinthika. Muli mbali imodzi ya ufumu tsopano. Ndinu mbadwa ya Ufumu wa Mulungu. Simulinso pansu pa mphamvu ya dziko lapansi:

Koma sitinalandira ife mzimu wa dziko lapansi, koma Mzimu wa kwa Mulungu, kuti tikadziwe zimene zipatsidwa kwa ife ndi Mulungu kwaufulu. (1 Akorinto 2:12).

Werengani zambiri za ufulu wanu mu Agalatiya 4:1-7.

MUZITETEZE NOKHA KU DZIKO

Popeza tsopano mwamasuka ku ukapolo wa dziko, dzitetezeni kuti makhalidwe a dziko asalowe m'moyo wanu. Musakhale ngati munthu wa dziko lapansi:

Penyani kuti pasakhale wina wakulanda inu ngati cuma, mwa kukonda nzeru kwace, ndi cinyengo copanda pace, potsata mwambo wa anthu, potsata zoyamba za dziko lapansi, osati potsata Kristu; (Akolose 2:8)

Musakonde dziko lapansi:

koma iye amene akasunga mau ace, mwa iyeyu zedi cikondi ca Mulungu cathedwa. M'menemo tizindikira kuti tiri mwa iye; (1 Yohane 2:15)

Musalole kuti mudetsedwe ndi nzeru za dziko lapansi:

Penyani kuti pasakhale wina wakulanda inu ngati cuma, mwa kukonda nzeru kwace, ndi cinyengo copanda pace, potsata mwambo wa anthu, potsata zoyamba za dziko lapansi, osati potsata Kristu; (Akolose 2:8)

Kanani zilakolako za dziko:

Ndi kutiphunzitsa ife kuti, pokana cisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo m'dziko lino odziletsa, ndi olungama, ndi opembedza; (Tito 2:12)

Khalani wosadetsedwa ndi dziko lapansi:

Mapembedzedwe oyera ndi osadetsa pamaso pa Mulungu ndi Atate ndiwo: z kuceza ndi ana amasiye ndi akazi amasiye m'cisautso cao, ndi 1 kudzisungira mwini wosacididwa mawanga ndi dziko lapansi. (Yakobo 1:27)

Pachikani mphamvu ya dziko:

Koma kudzitamandira ine konse konse, iai, koma mu mtanda wa Ambuye wathu Yesu Kristu, amene mwa iye dziko lapansi lapacikidwira ine, ndi ine ndapacikidwira dziko lapansi. (Agalatiya 6:14)

Imfa yopachikidwa si imfa wamba. Monga thupi, mphamvu ya dziko m'moyo wanu siifa imfa ya wamba. Mukuyenera kuipachika.

DZIWANI KUTI MUTHA KUGONJETSJA DZIKO LAPANSI

Simukuyenera kugonjetsedwa ndi dziko lapansi. Musalole zolabadira za dziko lapansi ziononge ntchito ya Mau m'moyo wanu (Mateyu 13:22; Marko 4:19). Malabadiro a zinthu za dziko ndi njira imodzi ya mzimu wa wokana Khristu (Daniel 7:25). Yesu anati:

Zinthu izi ndalankhula ndi inu, kuti mwa Ine mukakhale nao mtendere. M'dziko lapansi mudzakhala naco cibvuto, koma limbikani mtima; ndalilaka dziko lapansi Ine. (Yohane 16:33).

Mutha kugonjetsa dziko lapansi chifukwa Yesu amagonera mwa inu:

Inu ndinu ocokera mwa Mulungu, tiana, ndipo munailaka; pakuti iye wakukhah mwa inu aposa iye wakukhala m'dzi ko lapansi. Iwo ndiwo ocoken m'dziko lapansi; (1 Yohane 4:4)

Mungathe kuthawa chinyengo cha dziko lapansi:

mwa izi adatipatsa malonjezano a mtengo wace ndi akuru ndithu; kuti mwa izi mukakhale oyanjana nao umulungu wace, mutapulumuka ku cibvundi ciri pa dziko lapansi m'cilakolako. (2 Petro 1:4)

Mumagonjetsa dziko mwa kubadwa mwatsopano komanso ndi chikhulupiriro chanu:

Pakuti ciri conse cabadwa mwa Mulungu cililaka dziko lapansi; ndipo ici ndi cilako tililaka naco dziko lapansi, ndico cikhulupiriro cathu. (1 Yohane 5:4)

Mumagonjetsa dziko lapansi ndi mwanzi wa Yesu ndi umboni wanu:

Ndipo iwo anamlaka iye cifukwa ca mwazi wa Mwanawankhosa, ndi cifukwa ca mau a umboni wao; ndipo sanakonda moyo wao kungakhale kufikira imfa. (Chibvumbulutso 12:11)

MVETSETSANI UTUMIKI WANU KU DZIKO LAPANSI

Simukuyenera kusinthidwa ndi dziko lapansi koma kuti inu musinthe dziko lapansi. Wokhulupirira akuyenera kukhala kuunika kwa dziko la mdima lino, kuwalitsa ulemelero wa Mulungu ndi kugawa Uthenga Wabwino.

Inu ndi kuunika kwa dziko lapansi... (Mateyu 5:14)

Mphamvu ya utumiki wa mpingo woyamba pa dziko lapansi inali yaikulu kwambiri kufikira kuti ananenedwa kuti “asanduliza dziko lapansi dodolido” (Machitidwe 17:6).

Ngati asilikali omwe atumidwa kukagwira ntchito ku dziko lachilendo, okhulupiriranso ali atumidwa ku dziko lapansi ndi Mulungu kukagwira ntchito. Auzidwa kuti:

Pitani ku dziko lonse lapansi ndipo lalikirani Uthenga Wabwino ku cholengedwa chirichonse (Marko 16:15).

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Tanthauzirani mau oti “chenjerero”.

3. Tanthauzirani mau oti “njira zotsutsira machenjerero”

4. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira mu machenjerero a Satana kudzera mu dziko ndi thupi.

5. Lembani mwachidule njira zotsutsira machenjerero pogonjetsa dziko, thupi, ndi mdierekezi.

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukhu lino)

MACHITA CHITA A LUSO

1. Kupachikidwa inali njira yowawa kwambiri yofera. Werengani za kupachikidwa kwa Yesu mu Mateyu 27. Izi ndi zomwe zikuyenera kuchitika (wauzimu) ndi thupi, dziko komanso mphamvu yakumtima yolimbana ndi okhulupirira.
2. Tangodzifufuzani nokha komanso utumiki wanu. Kodi ndi mbali iti ya yomwe ikulamulidwa ndi dziko. Thupi? Satana? Kodi mungagwiritse ntchito motani zomwe mwaphunzira kugonjetsa mphamvu ya woipa m'madera amenewa?
3. Werengani Daniel 7:25. Kukopedwa ndi zolabadira za dziko ndi njira imodzi yodalirika ya wokana Khristu. Izi ndi zinthu zing'ono zing'ono zothodwetsa zomwe Satana amagwiritsa ntchito kufikira atakupangani kukhazikika mu zinthu za dziko lapansi osati za Mulungu. Kodi izi zikuchitika pa moyo wanu? Kumbukirani, ziphona za mphamvu sizitengeka ndi makopedwe a zinthu za dziko lapansi. Lingalirani ndi kupemphera momwe Mulungu angakuthandizireni kuti musakodwe ndi zolabadira za dziko lapansi.
4. Baibulo limafotokozerera moyo wa Chikristu ngati:
 - Moyo wogonjetsa: Aroma 8:37
 - Moyo wopambana: 1 Akorinto 15:57
 - Moyo wochuruka: Yohane 10:10
 - Moyo wa chipambano: 2 Akorinto 2:14
 - Moyo woyera: Aefeso 1:3-5; 5:25-27; 1 Petro 1:13:16

Izi ndi zomwe moyo wanu wauzimu ukuyenera kuyendamo tsiku ndi tsiku. Baibulo limafotokozerera za kulimbana mkati mwa moyo wa Paulo maka m'dera limeneli (Afilipi 3:12-17; Yakobo 1:2-4; Ahebri 12:10-16)

Munthu amakhalabe Mkhristu ngakhale akulimbanabe ndi vuto la uchimo pa moyo wake (1 Akorinto 5:1-5; 11:30-32; 1 Yohane 2:1-2) dziko (2 Timoteyo 4:10); kapena mphamvu ya ziwanda (Machitidwe 5:1-10; 1 Timoteyo 5:9-15; 3:6-7).

5. Pa Aefeso 4:22 ndi 24 Paulo akulankhula za munthu wakale yemwe akuyenera kuvulidwa, ndi munthu watsopano yemwe akuyenera kuvalidwa. Werengani Aefeso 4:22 – 6:18. Lembanani mndanda wa zinthu zomwe zikuyenera “kuvulidwa.” Lembaninso mndandanda wa zinthu zomwe zikuyenera kuvalidwa monga makhalidwe ndi malingiliro mwa zina.

ZOFUNIKA KUVULA

ZOFUNIKA KUVALA

CHAPUTALA 15 NKHONDO M'MAGANIZO

ZOLINGA

Pomaliza pa phunziro lino muzikwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kuzindikira bwalo leni leni la nkondo yauzimu
- Kufotokozera bwino tanthauzo la mau oti “mivi yoyaka moto” ya Satana
- Kuzindikira machenjerero a m'maganizo omwe Satana amagwiritsa ntchito pofuna kuthira nkondo maganizo.
- Kugwiritsa ntchito njira zotsutsira machenjerero pozimitsa “mivi yoyaka moto” imeneyi.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Pakuti pakuyendayenda m'thupi, siticita nkondo monga mwa thupi, (pakuti zida za nkondo yathu siziri za thupi, koma zamphamvu mwa Mulungu zakupasula malinga); ndi kugwetsa matsutsano, ndi cokwezeka conse cimene cidzikweza pokana ddziwitso ca Mulungu, ndi kugonjetsa ganizo lonse ku kumvera kwa Kristu (2 Akorinto 10:3-5)

MAU OYAMBA

Pamene Paulo amachenjeza Akhristu a ku Akorinto kuti asakhale osadziwa za machenjerero a Satana, mau oti “machenjerero” m'Chigriki ali ndi tsinde lofanana ndi mau oti “maganizo.” Mu njira ina Satana amalunjika maganizo a okhulupirira akafuna kuwathira nkondo. Maganizo ndi malo eni eni omwe nkondo yauzimu imachitikira. Nkondo iriyonse ya Satana imakhuza maganizo a munthu.

Chaputala chino chikukamba kwambiri za kumenyera nkondo maganizo. Imakambanso za machenjerero a Satana komanso njira zotsutsira machenjererowo kuti tikapambane pa nkondo yolimbana ndi mdierekezi. Nkondo ya maganizo yalembedwa mwachidule motere:

pakuti cisamaliro ca thupi ciri imfa; koma cisamaliro ca mzimu ciri moyo ndi mtendere. Cifukwa cisamaliro ca thupi cidana ndi Mulungu; pakuti sicigonja ku cilamulo ca Mulungu, pakuti sicikhoza kutero. (Aroma 8:6-7).

Satana amafuna atapanga maganizo anu kukhala achikunja (ochimwa, a chidzikodziko, a chithupithupi). Koma Mulungu amafuna maganizo anu akhale auzimu.

CHIFUKWA CHIMENE SATANA AMALIMBANA NDI MAGANIZO

Lamulo lalikuru lija limakambapo za kukonda Mulungu ndi nzeru zako zonse. Ichi ndi chifukwa chimodzi chimene iye amalimbana ndi maganizo:

Ndipo Yesu anati kwa iye, Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikuru ndi loyamba. (Mateyu 22:37-38)

Satana amalimbana ndi maganizo kapena nzeru zanu chifukwa zalumikizika kwambiri mwauzimu ku mtima wanu ndi pakamwa panu:

Munthu wozaza aputa makani; Koma wosakwiya msanga atonthoza makangano. Mayendedwe a wolesi akunga Hnga laminga, Koma njira ya oongoka mtima iundidwa ngati mseu. (Mateyu 15:18-19)

Satana amalimbana ndi nzeru zanu chifukwa makhalidwe anu amatengera maganizidwe anu:

Pakuti monga asinkha m'kati mwace, ali wotere; Ati kwa iwe, Idya numwe; Koma mtima wace suli pa iwe. (Miyambo 23:7)

Satana amadziwa kuti akayamba kulamulira maganizo anu, ndiye kuti athanso kulamulira thupi lanu, machitidwe anu, kenako mzimu wanu ngati saletsedwa.

MIVI YOYAKA MOTO YA MDANI

Mu Chipangano Chakale, mivi yoyaka moto imagwiritsidwa ntchito ngati zinthu za nkondo. Inali mabango okhala ndi mphako mkati momwe amaikamo zinthu zoti ziziyaka moto. Amadziyatsa kenako ndikuponya ndi mauta. Zinali zida zodalirika kwambiri maka ngati mzinda umene akufunawo uli ndi linga (mpanda) chifukwa amangoponya miviyo kudutsa pamwamba pa mpanda kukayatsa nyumba za dera la udzu mkatimo.

Pa Aefeso 6:11-17 Paulo akulankhula za nkondo yauzimu ndi Satana. Akulankhula za “mivi yoyaka moto ya woipayo.” Mdaniyo nthawi zonse amaponya mivi ya moto pa inu muuzimu. Ndipo mivi yambiri amailunjikitsa ku maganizo anu.

Mtumwi Paulo akuchenjeza kuti “musagwedezeke msanga m’maganizo” (2 Atesalonika 2:2). Kugwedezeka m’Chigriki ndi “kubalalika, kusokonezeka (ndiye kuti) kuonongeka.” Mukatenga chinthu ndi kuchigwedeza, ndiye kuti mukuchilamulira. Satana amagwifuna kukugwedezani kapena kukulamulirani.

CHENJERERO LA SATANA: NKHONDO M’MAGANIZO

Maganizo ndi gawo la thupi la munthu lomwe ndi lozama kwambiri komanso limene anthu salimvetsa. Chifukwa chakuti ndi lozama, Satana ali njira zochenjera zambiri zimene amagwiritsa ntchito kuthira nkhondo maganizo. Ngakhale kuti ndi zovuta kulemba njira zonsezo, mndandanda uli mmusiwu ukulemba mwachidule zina mwa njira zimene Satana amagwiritsa ntchito polimbana ndi maganizo a munthu:

KUDELERA ULAMULIRO WA MULUNGU

Yesero la munthu loyambirira linachitika m'maganizo. Linayamba ndi njira iyi: Kudelera ulamuliro wa Mulungu. Satana anati kwa Hava, “Eya, kodi Mulungu wanena kuti...? Mulungu ananenadi kuti musadye chipatse cha mu mtengo wodziwitsa zambino ndi zoipa? Kudelera kapena kufunsa mafunso pa zomwe Mulungu walankhula kumabweretsa chikaiko, ndi kusakhulupirira.

CHINYENGO NDI KUKOPA

Chinyengo inalinso njira ina ya machenjejerero a Satana. Iye atakumana ndi Hava, anazidzimbaitsa ngati njoka yokongola. Satana amagwiritsa ntchito mabodza, matsenga ndi “mizimu ya chipembedzo” kuti anyenge miyanda miyanda ya anthu pa dziko lapansi lero. Mu chinyengo cha Satana mumapezeka zinthu izi zokopa izi:

- “Utha kufanana ndi Mulungu.”
- “Utha kumadziwa za mtsogolo.”
- “Tsogolo lako Mulungu analikonza kale. Sungalisinthe.”
- “wina aliyense ndi mwana wa Mulungu.”
- “Kuli njira zambiri zopitira kumwamba si Yesu yekha.”
- “Mulungu ndiwabwino kwambiri sangaponye munthu ku Gahena.”
- “Zomwe Mulungu akungofuna pa iwe ndi kukhala moyo wabwino ndi kuyesesa kuchita zinthu zabwino.”
- “Baibulo silikuyenera kuwerenga ngati buku wamba.”
- “Baibulo liri ndi zolakwika zambiri.”

Mizimu yokopa ya Satana imathira nkhondo maganizo a munthu kusokoneza choonadi cha Mau a Mulungu:

Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m'masiku otsiriza ena adzataya cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunziro a ziwanda, (1 Timoteyo 4:1)

Satana anayesera kugwiritsa ntchito njira pomuyesa Yesu mu Luka 4:9-12. Amafuna kumpangitsa Yesu kuti adziponye yekha pansu kuchokera pachindwi cha kachisi popeza Mulungu walonjeza ku:

(...lamulira angelo ake pa iwe, akunyamule mmanja mwawo... (Luka 4:10-11).

THUPI

Mwaphunzira kale za thupi ngati chida cha mphamvu za kumdima. Satana amagwiritsa ntchito thupi kulimbana ndi maganizo:

koma ndiona lamulo lina m'ziwalo zanga, lirikulimbana ndi lamulo la mtima wanga, ndi kundigonjetsa kapolo wa lamulo la m'ziwalo zanga. (Aroma 7:23)

Satana amagwiritsa ntchito pakamwa panu, maso anu, makutu, ngakhale kukhudza ndi kununkhiza kuti aike maganizo oipa m'mutu mwanu.

KUCHITITSA KHUNGU MAGANIZO A OSAKHULUPIRIRA

Satana amaphimba maganizo a osakhulupirira kuti asaone choonadi cha Uthenga Wabwino:

mwa amene mulungu wa nthawi yino ya pansi pano unacititsa khungu maganizo ao a osakhulupirira, kuti ciwalitsiro ca Uthenga Wabwino wa ulemerero wa Kristu, amene ali cithunzithunzi ca Mulungu, cisawawalire. (2 Akorinto 4:4)

KUPSINJIKA

Kupsinjika ndiko kukhumudwa, kubalalika m'maganizo kapena kugwa nkhope. Zimapangitsa kuti munthu akhale wosowa mtendere, wopanda chiyembekezo komanso wosasangalala. Kupsinjika kutha kumpangitsa munthu kuyamba kuganiza zodzipha kapena kudzipha kumene chifukwa amamva kukhala opanda chiyembekezo zomwe zimabweretsa chisoni cha m'maganizo chosatha, litsipa ndi kulira.

Nthawi zina Satana amagwiritsa ntchito nyengo za moyo uno kubweretsa kupsinjika. Mwachitsanzo, kutaya kanthu kapena kuopa kutaya kanthu, mkwiyo woponderezedwa, kudzimva kuperewera, ziyembekezo zosakwaniritsidwa, ndi kuona zinthu mosakhala bwino, zonsezi zitha kubweretsa kupsinjika. Pa Miyambo 24:10 timachenjezedwa za “kukhumudwa pa tsiku la mdani” (nyengo zopsinja).

Pena kupsinjika kumabwera chifukwa cha maganizo osakhala bwino a iwo otizungulira omwe Satana amagwiritsa ntchito. Pa Deuteronomu 1:28 anthu a Mulungu anavomereza, “abale athu akumudwitsa mitima yathu.”

Timawerenga pa Numeri 21:4 kuti mtima wa anthu a Mulungu unakhumudwitsidwa kwakukuru. Davide nthawi zambiri amaonetsera kukhumudwa mu Masalimo ake (onani Masalimo 69 mwachitsanzo). Mtumwi Paulo pena anali nazo nyengo za kukhumudwa kwakukuru:

Pakuti sitifuna abale, kuti mukhale osadziwa za cisautso cathu tinakomana naco m'Asiya, kuti tinathodwa kwakukuru, koposa mphamvu yathu, kotero kuti tinada nkhwana ngakhale za moyo wathu; (2 Akorinto 1:8)

Ngati simugonjetsa kupsinjika zitha kubweretsa kuzunzika ndi mizimu ya Satana. Ili ndi gawo lozama la kupsinjika lomwe Satana amakhala ndi mphamvu zambiri pa maganizo a munthu.

KUKHUMUDWA

Kukhumudwa kumatanthauza kukhala “wopanda kulimbika mtima.” Satana amafuna kukukhumudwitsani chifukwa amadziwa kuti mukakhala opanda chilimbikitso, mukhala opanda mphamvu ku nkondo.

KUDZIPATULA

Njira ina yomwe Satana amagwiritsa ntchito ndiyodzipatula. Cholinga cha njira iyi ndiyokupangani kukhala munthu kudzisiyanitsa ndi thupi lonse la Khristu. Popeza kuti okhulupirira amagwira ntchito ngati thupi limodzi, kudzipatula kumakupangitsani kuti musachite kanthu. Zitsanzo zina za anthu a Mulungu omwe anathiridwa nkondo mu njira iyi ndi monga Eliya (1 Mafumu 19) ndi Yona (Yona 4:5-11).

ZOLINGA ZOLAKWIKWA

Munthu akamachita zinthu amakhala ndi zolinga. Izi ndi zofunika kuziona bwino chifukwa munthu amaona kunja (zochitika) koma Mulungu amayang'ana mtima:

Ndipo Sauli anati kwa anyamata ace, Mundifunire tsono munthu wakudziwa kuyimba bwino, nimubwere naye kwa ine. (1 Samuel 16:7)

Yesu sanadzipere kwatunthu kwa iwo chifukwa anadziwa anthu onse.

Koma Yesu sanakhulupirira iwo kuti akhale nao, cifukwa iye anadziwa anthu onse, ndipo sanasowa wina acite umboni za munthu; pakuti anadziwa iye yekha cimene cinali mwa munthu. (Yohane 2:24-25)

Anthu ambiri amayamba utumiki ndi zolinga zolakwika. Mulungu amaona kwambiri zolinga zolowera utumiki kusiyana ndi utumiki womwe mukuchita. Apa ndi pomwe nanunso mukuyenera mupaonetsetse bwino popeza kuti zolinga zanu zikakhala zabwino utumiki umayendanso bwino. Zolinga zanu pa utumiki zikuyenera kukhala zabwino:

Wetani gulu la Mulungu liri mwa inu, ndi kuliyang'anira, osati mokangamiza, koma mwaufulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyansa, koma mwacangu; osati

**monga ocita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo.
(1 Petro 5:2-3)**

Mukuyenera kulowa utumiki mosakakamizidwa, osatinso chifukwa cha phindu lomwe mungalipeze kapenanso kufuna udindo. Mukhale moyo wa chitsanzo. Satana adzayesetsa kuika zolinga zolakwika pa utumiki m'maganizo mwanu koma mochenjera kwambiri. Mwina atha kuika zolinga zokhumba mphamvu yolamulira anthu mu utumiki. Mutha kupeza chitsanzo cha izi pa Machitidwe 8:18-23 mu nkhani ya munthu wina wotchedwa Simon.

Mutha kukhala ndi zolinga zofuna kubwezera chilango munthu wina mu zochita zanu. Zitsanzo za m'Baibulo ndi monga Yona wofunitsitsa kuti Nineve aonongeke (Yona 4) komanso ophunzira a Yesu kufuna kuitanitsa moto kuchoka kumwamba (Luka 9:54).

Davide nayenso anali ndi zolinga zolakwika pofuna kudziwa chiwerengero cha anthu:

**Pamenepo Satana anaukira Israyeli, nasonkhezera Davide awerenge Israyeli.
(1 Mbiri 21:1)**

MAGANIZO OLAKWIKI NDI KUMVA M'MOYO

Satana amatha kutipanga kukhala ndi maganizo olakwika pa ena. Amaika mivi ya moto ya nsanje, kaduka, kukaikirana, kusakhulukira, mkwiyo, madano, kusagwirizana, kuganizirana zabodza, kupikisana, kusaleza mtima, kuweruzana, kutsutsa mochititsana manyazi, kusilira ndi kudzikonda.

Amayeranso kubweretsa maganizo olakwika a umbombo, kusakhutitsidwa, matama, kudziyenerenza, kutama maphunziro, kudzilungamitsa. Maganizo olakwika amabweretsa zomva mmoyo zosakhala bwino ndipo zonsezi zimachokera mmaganizo anu.

Zonsezi zimakupangani kukhala wopanda mphamvu pomenya nkondo yauzimu. Mwachitsanzo, Yakobo 4:6 amaonetsa kuti "Mulungu amakanitsa odzikuza." Ukadzadzidwa ndi kudzitamandira, umakhala ukudziika pa mzere wofuna kumenyana ndi Mulungu.

KUGALUKIRA

Satana amaikanso maganizo ogalukira m'maganizo mwanu. Kuukira ndiko kusamvera ulamuliro wa Mulungu mwadala. Kuukira kumakamba za kufuna za iwe mwini, kusayeruzika, kusamvera. Kumbukirani kuti tchimo loyamba la Satana ndikuukira. Kulankhula kwake kasanu nkumati, "Ndiza..." kumaonetsera kuukira (Yesaya 14:12-14). Mau oti "ndidza" ndi njira imodzi yodziwira kuti Satana akugwira ntchito mwa uyu kudzera mu mzimu woukira.

ZONENA NDI ZOTSUTSA

Satana amatchedwa “woneneza abale” (Chibvumbulutso 12:10). Amatumiza mivi yoyaka moto ya kuneneza m’aganizo mwanu, kukupanga kudzimva wopanda pake, ndi kutsutsuni. Amakupatsani chikumbumtima chochimwa ndi cha manyazi, kukhala wopanda pake ndi wonyazitsidwa.

Chinthu chimodzi chodziwira kutsutsidwa kwa Satana ndi kwa Mzimu Woyera ndikuti mukumbukire kuti Satana alibe chindunji. Mwachitsanzo, atha kumangolankhula zoti, “Iwe ndiye siwabwino,” “Sungakwanitse kukhala moyo wa Chikhristu,” “Mulungu sangakukonde chifukw ndiwe wochimwa kwambiri.”

Pamene kutsutsa kwa Mzimu Woyera kumakhala kwachindunji. Mwachitsanzo, amatha kungokupangani kuti muone vuto lanu leni leni kaya ndi mkwiyo kapena kusakhulupirika ndi zina.

CHIDETSO CHA CHIWEREWERE

Satana amatha kuika maganizo a chiwerewere, kusilira, kapena kumaganiza zogonana. Yesu anati:

koma Ine ndinena kwa inu, kuti yense wakuyang'ana mkazi kumkhumba, pamenepo watha kucita naye cigololo mumtima mwace. (Mateyu 5:28)

CHISOKONEZO

Satana amapangitsanso chisokonezo ndi kubalalika m’aganizo. Munthu akasokonezeka, kukhala kakasi komanso kubalalika, sangakhale msilikari wabwino wa Yesu.

MALINGILIRO OZUNZA

Pali malingiliro ambiri ozunza omwe Satana amatumiza m’mutu mwanu ngati mivi yoyaka moto monga kudandaula, nkhwana, chisoni, kusatsimikizika, ndi mantha. Malingiliro ozunzawa amatha kubweranso chifukwa cha kusaupeza mtima kapena kusowa poyambira chinthu.

Malingiro ozunzawa amatha kukhala mantha. Paulo akukamba za “mzimu wa mantha” mu 2 Timoteyo 1:7 ndi kuopa imfa mu Ahebri 2:15. Umu mulinso kuwawidwa mtima ndi zinthu zomwe zinachitika kale kale zoti zitha kukhululukidwa ndi kuiwalidwa.

KUNYENGELERA

Kunyengelera ndi kupanga mfundo ziwiri zotsutsana kuti zigwirizane. Mfundo za Mulungu ndi za Satana zimatsutsana. Satana amafuna kuti mutsitseko pang’ono mfundo zauzimu kuti zigwirizane ndi zake. Mwachitsanzo, atha kukuuzani kuti kukhala woyera kwambiri sikoyenera kapena kupeputsa Mau a Mulungu, mwa zina.

KUIKA MALINGILIRO POLAKWIKA

Satana adzayesetsa kukupangani kuti muike maganizo anu pa zinthu za dziko lapansi osati zamuyaya.

Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko apansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, cikondi ca Atate Isiciri mwa iye. (1 Yohane 2:15)

Malabadiro a dziko lapansi atha kupangitsa Mau a Mulungu kuti asakhale amphamvu m'moyo wanu. (Onani fanizo la ofesa mu Mateyu 13, Marko 4, ndi Luka 8). Zolabadira za dziko lino zitha kukuiwalitsani zakuti Yesu akubwera posachedwa.

Koma mudziyang'anire nokha, kuti kapena mitima yanu ingalemetsedwe ndi madyaidya ndi kuledzera, ndi zosamalira za moyo uno, ndi kuti tsiku ilo lingafikire inu modzidzimutsa ngati msampha; (Luka 21:34)

Satana atha kudzadza malingiliro anu ndi zachuma zokhazokha osati zinthu zamuyaya. Werengani fanizo la munthu wosauka ndi wolemera mu Luka 12:16-21:

Pakuti muzu wa zoipa zonse ndiwo cikondi ca pa ndalama; cimene ena pocikhumba, anasocera, nataya cikhulupiriro, nadzipyoza ndi zowawa zambiri. (1 Timoteyo 6:10)

Paulo akuchenjeza kuti ambiri aika maganizo awo pa zachuma cha dziko lapansi

Pakuti ambiri amayenda, za amene ndinakuuzani kawiri kawiri, ndipo tsopanonso ndikuuzani ndi kulira, ali adani a mtanda wa Kristu; citsiriziro cao ndico kuonongeka, mulungu wao ndiyo niimba yao, ulemerero wao uli m'manyazi ao, amenealingirira za padziko. (Afilipi 3:18-19)

KUSOKONEZEKA KWA MUTU

Mukalola Satana kuti achite ufumu mwa m'maganizo anu ndi kukhumudwa, malingiliro ofuna kudzipha ndi zina mutu wanu utha kusokonezeka mpaka ngati mwachita misala. Satana amanyamula maganizo a osakhulupirira ndi obwelera m'mbuyo; omwe anamdziwa kale Mulungu ndi kumsiya. (Muphunzira zambiri za izi mu Chaputala 21).

ZOTSUTSA MACHENJERERO ZAUZIMU CHIGONJETSO M'MAGANIZO

Satana amalimbana kwambiri ndi maganizo. Ngati munthu sachitapo kanthu pa maganizo oipa, atha kuchimwa. Machitsanzo, chidani kutha kuthera ku kupha. Malingaliro a chiwerewere atha

kuthera ku chigololo. Kutha kwa ukwati kumayambira m’ malingiliro. Kusilira kutha kumpanga munthu kuti abe.

Palibe kukaika... gawo lalikulu la nkondo ndi Satana limachitika m’ malingiliro. Koma musaope! Mulungu watipatsa njira zamphamvu zoti titsutsire machenjerero a Satana pa maganizo athu:

LOLANI MZIMU WOYERA AFUFUZE MAGANIZO ANU

Mundisanthule, Mulungu, nimudziwe mtima wanga; Mundiyeze nimudziwe zolingalira zanga. Ndipo mupenye ngati ndiri nao mayendedwe oipa, Nimunditsogolere pa njira yosatha. (Masalimo 139:23-24)

Pamene Mzimu Woyera abvumbulutsa zinthu kwa inu, chitani monga mwa bvumbulutsolo. Pemphani chikhululukiro pa malingiliro oipa ndi kugwiritsa ntchito Mau a Mulungu kuti mubadwitse malingiliro atsopano.

GWIRITSANI NTCHITO ZIDA ZANU ZA UZIMU

Magawi awiri a zida omwe angateteze malingiliro anu ku nkondo ya mdierekezi alembedwa mu Aefeso 6:16-17. Gawo limodzi la zida ndi chisoti cha chiyembekezo cha chipulumutso. Chisoti chimavaliidwa kumutu ndipo chimaimilira kutetezedwa kwa mutu.

Paulo sakulankhula za chipulumutso chanu mwa Yesu chomwe chitha kuyeretisa malingiliro anu ayi, komanso chipulumutso cha mtsogolo.

.... pakuti chipulumutso chathu chayandikira tsopano kuposa muja tinayamba kukhulupirira (Aroma 13:11).

Chipulumutso ndi chiyembekezo chanu cha tsogolo. Mkhristu yemwe ali ndi “chisoti cha chipulumutso” amadziwa kuti Mulungu agwira ntchito yokwaniritsa cholinga chake cha chipulumutso cha muyaya. Sadzidzimuka ndi nkondo za mdierekezi za m’ malingiliro. Amakhala ndi chiyembekezo osati cha lero chokha, komanso cha mtsogolo.

Gawo lina la zida zoteteza malingiliro anu ndi chikopa cha chikhulupiriro. Monga mwaphunzira kale, chikopa chimapangidwa ndi zinthu zolembera ndipo msilikari amanyamula kuika kutsogolo kwake kuti adziteteteze ku mivi ya adani. Miyiyo imangofikira pa chikopa kenako kugwa panso osamvulaza konse.

Chikopa cha msilikari wa Chikhristu chimatchedwa “chikopa cha chikhulupiriro.” Mau akuti “chikhulupiriro” satanthauza choonadi cha Mau a Mulungu chokha ayi koma kudalira kwanu mwa Mulungu. Gawo lina la zida za Mulungu ndi “lamba la choonadi” (Aefeso 6:14). Choonadi

cha Mau a Mulungu chimagonjetsa kutsutsidwa konse komwe mdani amabweretsa m'malingiliro mwanu.

GWIRITSANI NTCHITO MAU A MULUNGU

M'mayesero a Yesu pamene Satana anagwiritsa ntchito Mau a Mulungu, Yesu anagwiritsa ntchito Mau kuthana naye. Satana amabweretsa chikumbumtima chokutsutsa.

**Cifukwa cace tsopano iwo akukhala mwa Kristu Yesu alibe kutsutsidwa.
(Aroma 8:1)**

Satana akabwera ndi maganizo ozunza a mantha, gwiritsani ntchito malemba awa:

Mulibe mantha m'cikondi; koma cikondi cangwiro citaya kunja mantha, popeza mantha ali naco cilango, ndipo wamanthayo sakhala wangwiro m'cikondi. (1 Yohane 4:18).

Pakuti Mulungu sanatipatsa mzimu wa mantha; komatu wa mphamvu ndi cikondi ndi cidziletso. (2 Timoteyo 1:7)

Satana akafuna kukugwetsani ulesi, gwiritsani ntchito vesi ili:

Kodi sindinakulamulira iwe? Khala wamphamvu, nulimbike mtima, usaope, kapena kutenga nkhawa, pakuti Yehova Mulungu wako ali ndi iwe kuli konse umukako. (Yoswa 1:9)

Satana akabwetsa chikumbumtima chabodza m'malingiliro mwanu, kumbukirani...

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:9)

... ndipo gwiritsani ntchito mavesi onse okhuzana ndi malingiliro omwe mwapatsidwa m'phunziro lino kuti mumenye nkhondo ndi machenjerero a Satana pa maganizo anu.

LENGEZANI ZA MAGANIZO A MTENDERE

Lengezani za maganizo a mtendere pa moyo wanu ngati chifuniro chake cha Mulungu pa inu. Kuti muthane ndi malingiliro ozunza, lankhulani mtendere womwe ndi wanudi.

Mtendere ndikusiyirani inu, mtendere wanga ndikupatsani; Ine sindikupatsani inu monga dziko lapansi lipatsa. 5 Mtima wanu usabvutike, kapena usacite mantha. (Yohane 14:27)

Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana cidziwitso conse, udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Kristu Yesu. (Afilipi 4:7)

Izi ndi zitsanzo za momwe mungakuzire zida zanu za malemba polimbana ndi mdierekezi yemwe amathira nkhondo maganizo anu nthawi zonse. Pamene muwerenga Mau a Mulungu, pitirizani kuona mavesi omwe angateteze maganizo anu ku machenjerero a mdierekezi.

LOLANI MAGANIZO A KHRISTU AKHALE MWA INU

Paulo, mouziridwa ndi Mzimu Woyera:

Mukhale nao mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Kristu Yesu, (Afilipi 2:5)

Mau oti “lolani” amatanthauza kuvomera. Mukuyenera kulola maganizo anu kuti afanane ndi maganizo a Khristu. Kodi maganizo a Yesu anali otani? Ntchito ya kafukufuku wa funso ili yaperekedwa mu chigawo cha “Machitachita a Luso” cha phunziro lino. Ndizotheka kuchita izi, popeza Paulo analemba...

... koma ife tili ndi maganizo a Khristu (2 Akorinto 2:16).

KUDZIMANGA M'CHIUNO M'MAGANIZO ANU

Mu thupi, chiuno ndi tsinde la thupi lonse. M'chiuno ndi gawo lamphamvu kwambiri la thupi la munthu. Petro akulankhula kuti mukonzekeretse maganizo anu akhale amphamvu. Ichi, ndi chinthu choti muchite.

MANGANI UKAPOLO MAGANIZO OLAKWIKWA

Timauzidwa kuti titenge ukapolo maganizo onse kukumvera kwa Khristu (2 Akorinto 10:5). Maganizo akanakhala kuti si mdani, panalibe chifukwa chowatenga ukapolo. Taganizani momwe msilikari amamtengera munthu ukapolo ku thupi. Gwiritsani ntchito nzeru zomwezo potenga ukapolo maganizo anu ukapolo.

CHOTSANI MAGANIZO OIPA

Njira imodzi yotsutsira machenjerero pa maganizo anu ndi kuchotsa. Kuchotsa chinthu ndiko kutaya ndi mphamvu. Paulo anati:

Pakuti pakuyendayenda m'thupi, siticita nkhondo monga mwa thupi, (pakuti zida za nkhondo yathu siziri za thupi, koma zamphamvu mwa Mulungu zakupasula malinga); ndi kugwetsa matsutsano, ndi cokwezeka conse cimene cidzikweza pokana ddziwitso ca Mulungu, ndi kugonjetsa ganizo lonse ku kumvera kwa Kristu; (2 Akorinto 10:3-5)

Mukuyenera kuchotsa malingiliro onyasa omwe Satana amaika m'maganizo mwanu. Kuchotsa malingiliro omwe amadzikuza okha pamwamba pa Mulungu. Mukuyenera kubweretsa ku ukapolo ganizo liri lonse kukumvera Khristu.

Mumachotsa potenga ulamuliro pa maganizo anu ndi kukana kukhazikika pa zomwe Satana akuikiza mwa inu. Kumbukirani kuti mwauzidwa kuti muchotse. Si zinthu zoti Mulungu akuchitirani ayi.

LINGALIRANI ZINTHU IZI:

Njira imodzi yodzimangira m'chiuno m'maganizo anu ndikulingalira zinthu zinthu zabwino. Paulo anati:

Cotsalira, abale, zinthu ziri zonse zoonā, ziri zonse zolemekezeka, ziri zonse zolungama, ziri zonse zoyera, ziri zonse zokongola, ziri zonse zimveka zokoma; ngati kuli cokoma mtima cina, kapena citamando cina, zilingirireni izi. (Afilipi 4:8)

KONZANINSO MALINGILIRO ANU

koma kuti 1 mukonzeke, mukhale atsopano mu mzimu wa mtima wanu, (Aefeso 4:23)

Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro. (Aroma 12:2)

Konzani maganizo anu ndi pemphero komanso kulingilira Mau a Mulungu.

MUDZILIMBIKITSE NOKHA MWA AMBUYE

Davide anadzilimbikitsa yekha mwa Ambuye:

Ndipo Davide anadololoka kwambiri, pakuti anthu ananena za kumponya iye miyala, pakuti mtima wao wa anthu onse unali ndi cisoni, yense cifukwa ca ana ace amuna ndi akazi. Koma Davide anadzilimbikitsa mwa Yehova Mulungu wace. (1 Samuel 30:6)

Apanso, muchita kutengapo mbali. Mukuyenera kudzilimbikitsa nokha mwa Mulungu. Musadikire anthu ena kuti akuchitireni. Mudzilimbikitse nokha mothandizidwa ndi Mulungu.

ZINDIKIRANI TSINDE LA CHISOKONEZO

Pakuti Mulungu sali Mulungu wa cisokonezo koma wa mtendere; monga mwa Mipingo yonse ya oyera mtima. (1 Akorinto 14:33)

Popeza chisokonezo si cha Mulungu, musavomereze ganizo la chisokonezo m'malingiliro anu.

LAMULIRANI ZIPATA:

M'nthawi za Chipangano Chakale mizinda imazunguliridwa ndi malinga (mipanda) yodziteteza ku mphamvu za adani. Malingawo amakhala ndi zipata momwe mumaikidwa alonda omwe amakhala ndi ulamuliro wa polowera. Amene amakhala ndi ulamuliro wa polowera ndiye amakhala ndi mphamvu pa mzindawo.

Zimakhalanso choncho poteteza malingiliro anu. Zipata za mkati mwanu ndi kuona, kulawa, kununkhiza, kukhudza, ndi kumva. Musalole kanthu kali konse komwe kali ndi kuthekera kokuchimwitsani kuti kalowe mwa inu kudzera mu zipata izi. Ndiye kuti mukuyenera kutenga ulamuliro pa thupi lanu la uchimo.

Pewani zinthu zomwe zitha kutsegula zipata zolowera m'malingiliro anu. Izi ndi monga mowa ndi mankhwala ozunguza bongo zomwe zimasokoneza kachitidwe kanu ka zinthu. Kanema ndi zithunzi zolaula zimayambitsa maubwenzi auchimo ndi milandu yogwilira. Mitundu ina ya nyimbo, ufiti, nyanga, ndi zina zimatsegula zipata za maganizo anu.

Bvulani ntchito zonse za thupi ndipo mulole Mulungu akuze mwa inu chipatso cha Mzimu Woyera (onani Agalatiya 5:19-26). MUSAGONJERE ku nkondo za m'maganizo zomwe mdierekezi amabweretsa pa inu. Mukagonjera, Mulungu atha kukusiyani. Onani Aroma 1. Nthawi zina Mulungu amapereka anthu ku zomwe iwo eni adziperekako. Mupempheni Yesu akuthandizeni. Kumbukira uneneri wokamba za Yesu kuti “adzatenga ulamuliro pa zipata za mdani wake.” Muloleni atenge ulamuliro wa pa zipata zanu zauzimu.

KHAZIKITSANI MAGANIZO ANU PA MULUNGU:

Lolani maganizo anu akhazikike pa Mulungu:

Inu mudzasunga mtima wokhazikika mu mtendere weni weni, cifukwa ukukhulupirirani Inu. (Yesaya 26:3)

Lonjezano ili ndi lalikuru. Mukakhazitsa malingiliro anu pa Mulungu, mudzakhala ndi mtendere mkati mwa nkondo za mdani.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo.

2. Kodi bwalo lalikuru la nkhondo yauzimu ndi liti?

3. Kodi “mivi yoyaka moto” imatanthauza chiyani?

4. Lembani mwachidule machenjerero a mdierekezi pothira nkhondo malingiliro anu.

5. Lembani mwachidule njira zotsutsira machenjerero a mdierekezi pothira nkhondo malingiliro anu.

(Mayankho a mafunso awa ali kumapeto a bukhu lino)

MACHITACHITA A LUSO

1. Pa nkhondo ya maganizo, Satana amayesetsa kupangitsa:
 - Maganizo a chikunja: Aroma 8:6-7
 - Maganizo otalikirana ndi Mulungu mwa ntchito zoipa: Akolose 1:21
 - Maganizo odetsedwa: Tito 1:15
 - Maganizo a chithupithupi: Aefeso 2:3
 - Maganizo olimba ngati mwala: Daniel 5:20
 - Maganizo okaikira: Luka 12:29
 - Maganizo opanda pake: Aefeso 4:17
 - Maganizo ophimbika: 2 Akorinto 3:14
 - Maganizo ndi chikumbumtima chodetsedwa: Tito 1:15
 - Malingiliro opeputsa: Ezekiel 36:5
 - Malingiliro oipa: Machitidwe 14:2
 - Malingiliro osakhulupirira: 2 Akorinto 4:4
 - Malingiliro olema: Ahebri 12:3
 - Malingiliro ovunditsidwa: 2 Timoteyo 3:8
 - Kuganiza pawiri pawiri: Yakobo 1:8; 4:8
 - Maganizo achinyengo: 1 Timoteyo 6:5; 2 Timoteyo 3:8; 2 Akorinto 11:3
2. Maganizo oyenera kukhala nawo:
 - Maganizo okonzekeretsedwa: 2 Akorinto 8:19; 1 Petro 5:2; Machitidwe 17:11
 - Maganizo oyera: 2 Petro 3:1
 - Maganizo okhazikika: Yesaya 26:3
 - Maganizo okonzedwanso: Aefeso 4:23; Aroma 12:2
 - Maganizo odzichepetsa: Akolose 3:12; Machitidwe 20:19
 - Maganizo ofatsa: Tito 2:6
 - Maganizo abwino: 2 Timoteyo 1:7
 - Maganizo a chikondi: Mateyu 22:37.
 - Maganizo otumikira: Aroma 7:25
 - Maganizo otsimikizika: Aroma 14:5
 - Maganizo odzipereka: 2 Akorinto 7:7
 - Maganizo ofuna: 2 Akorinto 8:12
3. Chifukwa cha uchimo, anthu atha kukhala ndi maganizo osakonzekanso. Maganizo osakonzeka ndi oyipitsitsa kwambiri. Onani Aroma 1:28-32.
4. Monga mwaphunzira kale mu chaputala chino, imodzi mwa njira zopambanira pa nkhondo ya m'maganizo ndi kulola maganizo a Khristu akhale mwa ife. Werengani Chipangano Chatsopano kuti muone maganizo a Khristu. Kodi Yesu amaona zinthu motani? Kodi utumiki wake unaonetsera motani maganizidwe ake? Kodi ntchito zake zinaonetsera motani kaganizidwe kake.
5. Yesu amadziwa malingiliro a m'maganizo mwanu: Onani Luka 5:22; 6:8; 11:17.

6. Yerekezani 2 Samuel 13:28 ndi Yoswa 1:9. Onani kuti ndime ya mu Samuel ikufanana ndi ndime ya mu Yoswa pamene Mulungu akulankhula. Koma ndime ya mu Samuel imagwiritsidwa ntchito molakwika. Abisalomu analankhula mau amenewa kwa anthu omwe anapha m'bale wake, Amnoni. Satana amakhala woopsa kwambiri akamagwiritsa ntchito popeza amawasintha. Iyi ndi njira yaikulu yomwe amagwiritsa ntchito kusokeneza maganizo a anthu.

CHAPUTALA 16

NKHONDO YA LILIME

ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputala chino mukhala mukukwanitsa kuchit a zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
- Kuzindikira kuti lilime ngati bwalo lofunikira kwambiri la nkondo yauzimu.
- Kulemba mwachidule njira za Satana polamulira lilime.
- Kulemba mwachidule njira za zotsutsira machenjerero a Satana pa kumbana nkondo ya lilime.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

koma lilime palibe munthu akhoza kulizoloweretsa; liri coipa cotakataka, lodzala ndi ululu wakupha. (Yakobo 3:8)

MAU OYAMBA

Mu chaputala chapitachi mwaphunzira za maganizo ngati malo ofunikira kwambiri omenyerapo nkondo yauzimu. Zomwe zimachitika m'maganizo zimakhuza lilime ndipo lilime limakhuza mzimu, moyo, mtima, ndi thupi. Chaputala chino chikuona gawo lina lofunikira pa nkondo yauzimu, nkondo ya lilime.

ZOMWE BAIBULO LIMAKAMBA ZA LILIME

Musanayambe kuona za machenjerero a Satana pa lilime, werengani zomwe Baibulo likulankhula za lilime pa Yakobo 3:1-13. Mavesiwa akuonetsa kuti lilime ndi lamphamvu ngakhale ndi chiwalo chaching'ono pa thupi la munthu. Thupi lonse litha kudetsedwa chifukwa cha lilime. Lilime silingakonzeke ndi munthu. Ndi pokhapokha mwapanga lilime lanu kugonjera kwa Mulungu ndiye mutha kulilamulira. Komabe, zikhala zovuta kuti likonzeke. Simungatayirire pa kuyang'anira lilime lanu poganiza kuti mwaligonjetsa kotheratu.

Baibulo limayerekeza lilime ndi:

- Moto: Yakobo 3:5
- Moto woyaka: Miyambo 16:27
- Dziko la zoipa: Yakobo 3:6
- Chirombo chofunika kukonzedwa: Yakobo 3:7-8
- Kasupe wa madzi abwino kapena owawa: Yakobo 3:11
- Mtengo wobala zipatso zabwino kapena zoipa: Yakobo 3:12

- Choipa chosaweruzika: Yakobo 3:8
- Mankhwala oipa akupha: Yakobo 3:8
- Lumo lakuthwa: Masalimo 52:2
- Lupanga lakuthwa: Masalimo 57:4; 59:7
- Njoka ya ululu woipa: Masalimo 140:3
- Dzenje lakuya: Miyambo 22:14

Baibulo limati lilime lilime ndi lamphamvu chifukwa cha zomwe limachita pa ena. Lilime ndi mphamvu yobweretsa imfa kapena moyo:

Lilime liri ndi mphamvu pa imfa ndi moyo... (Miyambo 18:21).

Lilime ndi lamphamvu chifukwa cha zomwe limachita pa inu. Mutha kudzikola nokha ndi mau a mkamwa mwanu:

Wakodwa ndi mau a m'kamwa mwako, Wagwidwa ndi mau a m'kamwa mwako. (Miyambo 6:2)

Lilime ndi lamphamvu chifukwa litha kukusiyanyitsani inu ndi Mulungu:

Amene amati, Ndi lilime lathu tidzaposya; Milomo yathu nja ife eni; mbuye wa pa ife ndani? (Masalimo 12:4).

MACHENJERERO A SATANA: NKHONDO YA LILIME

Lilime lanu lalumikizika ku mtima wanu, thupi lanu, moyo wanu, ndi mzimu wanu. Mwachitsanzo, ngati Satana ali ndi ulamuliro pa mtima wanu, ndiye kuti ali ndi ulamuliro pa lilime lanu:

Koma zakuturuka m'kamwa zicokera mumtima; ndizo ziipitsa munthu. Pakuti mumtima mucokera maganizo oipa, zakupha, zacigololo, zaciwerewere, zakuba, za umboni wonama, zamwano; izi ndizo ziipitsa munthu, koma kudya osasamba manja sikuipitsa munthuai. (Mateyu 15:18-20)

kuti analowa m'nyumba ya Mulungu, natenga mikate yoonetsera, nadya, napatsanso iwo anali naye pamodzi; imeneyi yosaloledwa kudya ena koma ansembe okha? (Luka 6:45)

Satana amagwiritsa ntchito zinthu zomwe mumalankhula kuti apeze njira yolowera mkati mwanu:

Kuciza lilime ndiko mtengo wa moyo; Koma likakhota liswa moyo. (Miyambo 15:4)

Chifukwa cha kulumikizana koipa mumapereka mpata wakuti Satana alowe ndi kumenya nkhondo ndi mzimu wanu. Iye amagwiritsanso ntchito milomo yanu kuti aononge moyo wanu:

M'kamwa mwa wopusa mumuononga, Milomo yace ikhala msampha wa moyo wace. (Miyambo 18:7).

Wosunga m'kamwa mwace ndi lilime lace Asunga moyo wace kumabvuto. (Miyambo 21:23).

Satana amatha kufikira thupi lanu lonse kudzera mu lilime:

Ndipo lilime ndilo moto; ngati dziko la cosalungama mwa ziwalo zathu laikika lilime, ndili lodetsa thupi lonse, niliyatsa mayendedwe a cibadwidwe, ndipo liyatsidwa ndi gehena. (Yakobo 3:6)

Lilime lanu limakhudza moyo wanu wonse:

Wogwira pakamwa pace asunga moyo wace; Koma woyasamula milomo yace adzaonongeka. (Miyambo 13:3)

Satana amafuna kulamulira lilime lanu pokuyesani kuti mulankhule:

MAU OSILIRA

Mtima wanu ukhale wosakonda cuma; zimene muli nazo zikukwanireni; pakuti iye anati, Sindidzakusiya konse, kungakhale kukutaya, sindidzakutaya ndithu. (Ahebri 13:5)

MAU OPANDA PAKE

Ndipo ndinena kwa inu, kuti mau onse opanda pace, amene anthu adzalankhula, adzawawerengera mlandu wace tsiku la kuweruza. (Mateyu 12:36)

MAU OPUSA

Mtima wa wozindikira ufunitisa kudziwa; Koma m'kamwa mwa opusa mudya utsiru. (Miyambo 15:14)

MAU OPANDA PHINDU

Uwakumbutse izi, ndi kuwacitira umboni pamaso pa Ambuye, kuti asacite makani ndi mau osapindulitsa kanthu, koma ogwetsa iwo akumva. (2 Timoteyo 2:14)

MALAMULO NDI NTHANO ZA ANTHU

osasamala nthanu zacabe za Ciyuda, ndi malamulo a anthu opatuka kusiyana naco coonadi. (Tito 1:14)

ZOIPA ZA ZINTHU ZOMWE SIMUKUZIDZIWA

Koma iwowa zimene sazidziwa azicitira mwano; ndipo zimene azizindikira cibadwire, monga zamoyo zopanda nzeru, mu izi atayika, (Yuda 10)

Koma awo, ngati zamoyo zopanda nzeru, nyama zobadwa kuti zikodwe ndi kuonongedwa, akucitira mwano pa zinthu osazidziwa, adzaonongeka m'kuononga kwao, (2 Petro 2:12)

MAU OKOPA

Ici ndinena, kuti munthu asakusokeretseni inu ndi mau okopakopa. (Akolose 2:4)

KUNG'UNG'UDZA, KUDANDAULA, NDI KUNYADA

Amenewo ndiwo odandaula, oderera, akuyenda monga mwa zilakolako zao (ndipo pakamwa pao alankhula zazikuruzikuru), akutama anthu cifukwa ca kupindula nako. (Yuda 16)

Pakuti polankhula mau otukumuka opanda pace, anyengerera pa zilakolako za thupi, ndi zonyansa, iwo amene adayamba kupulumukira a mayendedwe olakwawo; (2 Petro 2:18)

MAU ACHABE

Amanena za bodza munthu yense ndi mnansi wace: Amanena ndi mlomo wotyasika, ndi mitima iwiri.(Masalimo 12:2)

MAU ONYADA

... ndi pakamwa pawo alankhula monyada (Masalimo 17:10)

MAU ODZITAMANDIRA

Anena mau, alankhula zawawa; Adzitamandira onse ocita zopanda pace. (Masalimo 94:4)

MAU OTCHULA DZINA LA MULUNGU PACHABE

(Eksodo 20:7)

MAU OTEMBELERA NDI OWAWA:

Yemwe mkamwa mwake mwadzadza mau otembelera ndi owawa (Aroma 3:14).

MABODZA

Oipa acita cilendo cibadwire: Asokera kuyambira kubadwa kwao, nanena bodza. (Masalimo 58:3)

Ikhale yosalankhula milomo ya mabodza, Imene imalankhula mwacipongwe pa olungama mtima, Ndi kudzikuza ndi kunyoza. (Masalimo 31:18)

MAU OLALATA

Ukhala, nuneneza mbale wako; Usinjirira mwana wa mai wako. (Masalimo 50:20)

MAU OTSITSA (MISECHE)

Munthu wokhota amautsa makani; Kazitape afetsa ubwenzi. (Miyambo 16:28)

MAU A UKAZITAPE

Kazitape woyendayenda amawanditsa zinsinsi; Koma wokhulupirika mtima abisa mau. (Miyambo 11:13)

MAU OSINJILIRA

Amene sasinjirira ndi lilime lace, Sacitira mnzace coipa, Ndipo satola msece pa mnansi wace. Amene sasinjilira ndi lilime lake... (Masalimo 15:3)

MAU OGAWA

Usayankhe citsiru monga mwa utsiru wace, Kuti ungafanane naco iwe wekha. (Miyambo 26:4)

MAU A MAKANI

Milomo ya wopusa ifikitsa makangano; Ndipo m'kamwa mwace muputa kukwapulidwa. (Miyambo 18:6)

MAU A MIKANGANO

Pobisalira pamaso panu mudzawabisa kwa ciwembu ca munthu: Mudzawabisa iwo mumsasa kuti muwalanditse pa kutetana kwa malilime. (Masalimo 31:20)

MAU ODANITSA

Mboni yonama yonong'ona mabodza, Ndi wopikisanitsa abale. (Miyambo 6:19)

MAU OMEZA

Ukonda mau onse akuononga, Lilime lacinyengo, iwe. (Masalimo 52:4)

MAU OKHOTAKHOTA NDI OPOTOKA

Miyambi 4:24 Tasiya m'kamwa mokhota, Uike patari milomo yopotoka. (Miyambo 4:24)

MAU OYIPA NDI ONYENGA

Pakamwa pako mpocita zocimwa, Ndipo lilime lako likonza cinyengo. (Masalimo 50:19)

MAU OWONONGA

Ndipo andichera misampha iwo akufuna moyo wanga; Ndipo iwo akuyesa kundicitira coipa alankhula zoononga, Nalingirira zonyenga tsiku lonse. (Masalimo 38:12)

MAU ONYASA

Koma tsopano tayani inunso zonsezi: mkwiyo, kupsa mtima, dumbo, mwano, zonyansa zoturuka m'kamwa mwanu: (Akolose 3:8)

NJIRA ZAUZIMU ZOTSUTSIRA MACHENJERERO CHIGONJETSO PA LILIME

Davide atazindikira za nkondo yaikuru ya lilime, analira nati:

Adzakuninkhanji, adzakuonjezeranji, Lilime lonyenga iwe? (Masalimo 120:3).

Njira yokhayo yopambanira nkondo ya lilime ndi yogwiritsa ntchito njira zotsutsira machenjerero zomwe zaperekedwa m'Mau a Mulungu.

PANGANI MTIMA WANU UKHALE BWINO NDI MULUNGU

Chomwe mungachite poyamba kuti mupambane pa nkondo ya lilime ndi kukonza mtima wanu pamaso pa Mulungu:

zakuturuka m'kamwa zicokera mumtima; ndizo ziipitsa munthu. Pakuti mumtima mucokera maganizo oipa, zakupha, zacigololo, zaciwerewere, zakuba, za umboni wonama, zamwano; izi ndizo ziipitsa munthu, koma kudya osasamba manja sikuipitsa munthuai. (Mateyu 15:18-20)

Pakamwa panu pamalankhula zomwe ziri mu mtima mwanu. Ngati mtima wanu suli bwino, lilime lanu liulura. Gwiritsani ntchito lilime lanu kupangitsa mtima wanu ukhale bwino ndi Mulungu:

kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka: pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo cilungamo; ndi m'kamwa abvomereza kutengapo cipulumutso (Aroma 10:9-10)

ZINDIKIRANI UDINDO WANU

Dziwani kuti mudzafunsidwa pa mau onse omwe amatuluka mkamwa mwanu:

Ndipo ndinena kwa inu, kuti mau onse opanda pace, amene anthu adzalankhula, adzawawerengera mlandu wace tsiku la kuweruza. Pakuti udzayesedwa wolungama ndi mau ako, ndipo ndi mau ako omwe udzatsutsidwa. (Mateyu 12:36-37)

Ananena kwa iye, Pakamwa pako ndikuweruza, kapolo woipa iwe. Unadziwa kuti ine ndine munthu wouma mtima, wonyamula cimene sindinaciika, ndi wotuta cimene sindinacifesa; (Luka 19:22)

DZIWANI KUTI MAU ANU AMAONETSERA UTHENGA WABWINO

Ngati simudziwa kuti lilime lanu ndi lofunika kwambiri, simutenga ulamuliro pa ilo. Zindikirani kuti malankhulidwe anu amaonetsera Uthenga Wabwino wa Yesu:

Cokhaci, mayendedwe anu ayenere Uthenga Wabwino wa Kristu: kuti, ndingakhale nditi ndirinkudza ndi kuona inu, ndingakhale nditi ndiri kwina, ndikamva za kwa inu, kuti mucirimika mu mzimu umodzi, ndi kugwirira pamodzi ndi moyo umodzi cikhulupiro ca Uthenga Wabwino; (Afilipi 1:27)

Chifukwa cha ichi mukuyenera kupereka chitsanzo chabwino pa malankhulidwe anu:

Munthu asapeputse ubwana wako; komatu khala citsanzo kwa iwo okhulupira, m'mau, m'mayendedwe, m'cikondi, m'cikhulupiriro, m'kuyera mtima. (1 Timoteyo 4:12)

Zomwe zimatuluka mkamwa mwanu anthu akunja amaziona:

Pamenepo pakamwa pathu panadzala ndi kuseka, Ndi lilime lathu linapfuula mokondwera; Pamenepo anati mwa amitundu, Yehova anawacitira iwo zazikuru, (Masalimo 126:2)

Muthanso kupindulira Khristu miyoyo kudzera m'malankhulidwe anu:

Momwemonso, akazi inu, mverani amuna anu ainu nokha; kuti, ngatinso ena samvera mau, akakodwe opanda mau mwa mayendedwe a akazi; pakuona mayendedwe anu oyera ndi kuopa kwanu. (1 Petro 3:1-2)

MAU AKHALE OCHEPA NDI OSAVUTA

Pocuruka mau zolakwa sisisoweka; Koma wokhala cete acita mwanzeru. (Miyambo 10:19)

Kama manenedwe anu akhale, Inde, inde; Iai, iai; ndipo coonjezedwa pa izo cicokera kwa woipayo. (Mateyu 5:37)

GANIZANI KAYE MUSANALANKHULE

Mudziwa, abale anga okondedwa, kuti munthu ali yense akhale wochera khutu, wodekha polankhula, wodekha pakupsa mtima. (Yakobo 1:19)

Ngati wapusa podzikweza, Ngakhale kuganizira zoipa, tagwira pakamwa. (Miyambo 30:32)

Mtima wa wolungama uganizira za mayankhidwe; Koma m'kamwa mwa ocimwa mutsanulira zoipa. (Miyambo 15:28)

Miyambi 17:28 Ngakhalecitsirucikatontholaaciyesa canzeru; Posunama ali wocenjera. (Miyambo 17:28)

DZIPATULENI NOKHA

Dzipatuleni kwa iwo amene satha kugwira lilime lawo:

Miyambi 14:7 Pita pamaso pa munthu wopusa, Sudzazindikira milomo yakudziwa. (Miyambo 14:7)

PHUNZIRANI MPHAMVU YA MAU A MTENDERE

Mau a mtendere ali ndi mphamvu kuposa mau a mkwiyo:

Cipiriro cipembedza mkuru; Lilime lofatsa lityola pfupa, (Miyambo 25:15)

ZINDIKIRANI KUTI LILIME LANU NDI CHIDA

Lilime lanu ndi chida chomwe mutha kugonjetsera mdani m'malo mogonjetsedwa:

Ndi kukhala naco cikumbu mtima cabwino, kuti umo akunenerani, iwo akunenera konama mayendedwe anu abwino m'Kristu akacidwe manyazi. (1 Petro 3:16)

LAMULIRANI LILIME LANU

Ndi thandizo la Mulungu, mutha kulamulira lilime lanu. Koma nkhani ndi yakuti mukuyenera kuchitapo kanthu INUYO. Mavesi otsatirawa akuonetsera ntchito yoti INUYO muchite:

Pakuti, iye wofuna kukonda moyo, Ndi kuona masiku abwino, Aletse lilime lace lisanene coipa, Ndi milomo yace isalankhule cinyengo; (1 Petro 3:10)

Aacitire mwano munthu ali yense, asakhale andeu, akhale aulere, naonetsere cifatso conse pa anthu onse. (Tito 3:2)

Musamanenerana, abale. Wonenera mbale, kapena woweruza mbale wace, anenera lamulo, naweruza lamulo: koma ngati uweruza lamulo, suliwocita lamulo, komatu woweruza. Woika lamulo ndi woweruza ndiye mmodzi, ndiye amene akhoza kupulumutsa ndi kuononga; koma iwe woweruza mnzako ndiwe yani? (Yakobo 4:11-12)

Mtima wanu ukhale wosakonda cuma; zimene muli nazo zikukwanireni; pakuti iye anati, Sindidzakusiya konse, kungakhale kukutaya, sindidzakutaya ndithu. (Ahebri 13:5)

Cokhaci, mayendedwe anu ayenere Uthenga Wabwino wa Kristu: kuti, ndingakhale nditi ndirinkudza ndi kuona inu, ndingakhale nditi ndiri kwina, ndikamva za kwa inu, kuti mucirimika mu mzimu umodzi, ndi kugwirira pamodzi ndi moyo umodzi cikhulupiriro ca Uthenga Wabwino; (Afilipi 1:27)

kuti mubvule, kunena za makhalidwe anu oyamba, munthu wakale, wobvunda potsata zilakolako za cinyengo; (Aefeso 4:22-25)

Koma tsopano tayani inunso zonsezi: mkwiyo, kupsa mtima, dumbo, mwano, zonyansa zoturuka m'kamwa mwanu: (Akolose 3:8)

Nkhani yonse yobvunda isaturuke m'kamwa mwanu, koma ngati pali yina yabwino kukumangirira monga mofunika ndiyo, 9 kuti ipatse cisomo kwa iwo akumva. (Aefeso 4:29)

komatu monga iye wakuitana inu ali woyera mtima, khaiani inunso oyera mtima m'makhalidwe anu onse; popeza kwalembedwa, Muzikhala oyera mtima, pakuti Ine ndine woyera mtima. (1 Petro 1:15-16)

Uletse lilime lako lisachule zoipa, Ndipo milomo yako isalankhule cinyengo. (Masalimo 34:13)

Ndinati, Ndidzasunga njira zanga, Kuti ndingacimwe ndi lilime langa: Ndidzasunga pakamwa panga ndi cam'kamwa, Pokhala woipa ali pamaso panga. (Masalimo 39:1)

Wopereka nsembe yacyyamiko andilemekeza Ine; Ndipo kwa iye wosunga mayendedwe ace Ndidzamuonetsa cipulumutso ca Mulungu. (Masalimo 50:23)

Usaehule dzina la Yehova Mulungu wako pacabe; cifukwa Yehova sadzamuyesa iye wosacimwa, amene achula pacabe dzina lace. (Eksodo 20:7)

Ndi kuwacitira cifundo anthu zikwizikwi a iwo amene akondana ndi Ine, nasunga malamulo anga. (Eksodo 20:6)

MALANKHULIDWE ANU ATENGERE A YESU

Yesu amalankhula mau a chisomo:

Ndipo onse anamcitira iye umboni nazizwa ndi mau a cisomo akuturuka m'kamwa mwace; nanena, Kodi uyu si mwana wa Yosefe? (Luka 4:22)

Analankhula mau a ulamuliro a Mulungu:

Ndipo anazizwa ndi ciphunzitso cace; pakuti anaphunzitsa monga mwini mphamvu, si monga alembi. (Marko 1:22)

Mkamwa mwake munalibe mau a chinyengo:

amene sanacita cimo, ndipo m'kamwa mwace sicinapezedwa cinyengo;(1 Petro 2:22-23)

GWIRITSANI LILIME LANU PA ZABWINO

Lankhulani mau a nzeru ndi a chisomo:

Atsegula pakamwa pace ndi nzeru, Ndipo cilangizo ca cifundo ciri pa lilime lace. (Miyambo 31:26)

Lankhulani za Mulungu:

**Ndidzalingalira ulemerero waukuru wa ulemu wanu, Ndi nchito zanu zodabwiza.
(Masalimo 145:5)**

Pakamwa panga padzafotokozerwa cilungamo canu, Ndi cipulumutso canu tsiku lonse; Pakuti sindidziwa mawerengedwe ace. (Masalimo 71:15)

Lilime langa lomwe lidzalankhula za cilungamo canu tsiku lonse: Pakuti ofuna kundicitira coipa acita manyazi, nadodoma. (Masalimo 71:24)

Lankhulani za Mau a Mulungu:

**Lilime langa liyimbire mau anu; Pakuti malamulo anu onse ndiwo olungama.
(Masalimo 119:172)**

**Ndidzalankhulanso za umboni wanu pamaso pa mafumu, Osacitapo manyazi.
(Masalimo 119:46)**

Lankhulani za mau a chitonthozo kuchokera m'Mau a Mulungu:

Chotero tonthozanani wina ndi mnzake ndi mau awa (1 Atesalonika 4:18)

Lankhulani za Ufumu wa Mulungu:

Adzanenera ulemerero wa ufumu wanu, Adzalankhulira mphamvu yanu;(Masalimo 145:11)

Milomo yanu idzadzidwe ndi matamando a Mulungu:

Pakamwa panga padzanena cilemekezo ca Yehova; Ndi zinthu zonse zilemekeze dzina lace loyera ku nthawi za nthawi. (Masalimo 145:21)

Nyimbo zakukweza Mulungu zikhale pakamwa pao, Ndi lupanga lakuthwa konse konse m'dzanja lao; (Masalimo 149:6)

Ndidzayimbira zacifundo za Yehova nthawi yonse: Pakamwa panga ndidzadzziwitsira cikhulupiriko canu ku mibadwo mibadwo. (Masalimo 89:1)

Ndidzayamika Yehova kwakukuru pakamwa panga; Ndi pakati pa anthu aunyanji ndidzamlemekeza. (Masalimo 109:30)

**Lilime langa liyimbire mau anu; Pakuti malamulo anu onse ndiwo olungama.
(Masalimo 119:172)**

Pakuti cifundo canu ciposa moyo makomedwe ace; Milomo yanga idzakulemekezani. (Masalimo 63:3)

Mudzakhutitsa moyo wanga ngati ndi mafuta ndi zonona; Ndipo pakamwa panga ndidzakulemekezani ndi milomo yakupfuula mokondwera; (Masalimo 63:5)

**Ndinampfuulira Iye pakamwa panga, Ndipo ndinamkuza ndi lilime langa,
(Masalimo 66:17)**

**M'kamwa mwanga mudzadzala lemekezo lanu, Ndi ulemu wanu tsiku lonse.
(Masalimo 71:8)**

Milomo yanga idzapfuula mokondwera poyimbira Inu Nyimbo; Inde, moyo wanga umene munaombola. (Masalimo 71:23)

Ndidzalemekeza Yehova nyengo zonse; Kumlemekeza kwace kudzakhala m'kamwa mwanga kosalekeza. (Masalimo 34:1)

MUSANALANKHULE DZIFUNSENI MAFUNSO AWA:

1. Kodi zimene ndilankhulezi zibweretse ulemelero kwa Mulungu?
Ndipo ciri conse mukacicita m'mau kapena muncbito, citani zonse m'dzina la Ambuye Yesu, ndi kuyamika Mulungu Atate mwa iye. (Akolose 3:17)
2. Kodi ndi choonadi ichi?
3. Kodi ndi zokomera onse okhudzidwa?
4. Kodi zikhala zopindulira onse okhudzidwa?
5. Kodi zimangilira ena (zibweretsa ubwino ndi ubale wabwino)?
6. Ngati mukulankhula za munthu wina, kodi iye mwamuuza kale zimenezi?
7. Kodi mwatsimikizika kuti zomwe mukulankhulazo ndi zoonza kapena ndi mphekesera chabe?
8. Ngati muli ndi mangawa ndi mnzanu, mwayesera kukamba naye kuti muyanjane musanauze munthu wina?
9. Kodi ndi zofunika ndithu kuti mulankhule zinthuzi?

KUMBUKIRANI MAVESI AWA:

**Pakuti asanafike mau pa lilime langa, Taonani, Yehova, muwadziwa onse.
(Masalimo 139:4)**

Wanzeru mtima adzachedwa wocenjera; Ndipo kukoma kwa milomo kuyenjezera kuphunzira. (Miyambo 16:21)

Munthu akondwera ndi mayankhidwe a m'kamwa mwace; Ndi mau a pa nthawi yace kodi sali abwino? (Miyambo 16:23)

Munthu akondwera ndi mayankhidwe a m'kamwa mwace; Ndi mau a pa nthawi yace kodi sali abwino? (Miyambo 15:23)

Popezaizi zonse zidzakanganuka kotero, muyenera inu kukhala anthu otani nanga, m'mayendedwe opatulika ndi m'cipembedzo, (2 Petro 3:11)

**Mau oyenera a pa nthawi yace Akunga zipatso zagolidi m'nsengwa zasiliva.
(Miyambo 25:11)**

m'kamwa mwace ndi lilime lace Asunga moyo wace kumabvuto. (Miyambo 21:23)

**pakamwa pace asunga moyo wace; Koma woyasamula milomo yace adzaonongeka.
(Miyambo 13:3)**

LENGEZANI MALONJEZANO AWA

**Imvani, pakuti ndikanena zoposa, Ndi zolungama potsegula pakamwa panga,
Pakuti m'kamwa mwanga mudzalankhula ntheradi, Zoipa zinyansa milomo yanga.
Mau onse a m'kamwa mwanga alungama; Mwa iwo mulibe zokhota ndi zopotoka.
(Miyambo 8:6-8)**

PEMPHERANI MAPEMPHERO AWA:

**Muike mdindo pakamwa panga, Yehova; Sungani pakhomo pa milomo yanga.
(Masalimo 141:3)**

**A m'kamwa mwanga ndi maganizo a m'mtima wanga abvomerezeke pamaso panu,
Yehova, thanthwe langa, ndi Mombolo wanga, (Masalimo 19:14)**

KHAZIKITSANI CHOLINGA ICHI:

**Mwayesera mtima wanga; mwandizonda usiku; Mwandisuntha, simupeza kanthu;
Ndatsimikiza mtima kuti m'kamwa mwanga simudzalakwa. (Masalimo 17:3)**

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo

2. Kodi mutu wa nkhondo yauzimu womwe wakambidwa mu chaputala ichi ndi wotani?

3. Tchulani njira zomwe Satana akufuna kuzigwiritsa ntchito pofuna kukugonjetsani mu nkhondo yauzimu?

4. Lembani mwachidule njira zotsutsira machenjerero a Satana pa lilime.

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukhu lino)

MACHITACHITA A LUSO

Mabuku a Masalimo ndi Miyambo ali ndi zambiri zolankhula pa za lilime.

1. Onani vesi iliyonse ya mu Miyambo. Yerekezani mau omwe ali m'mavesiwa. Muonere chitsanzo chaperekedwacho.

VESI	LILIME LABWINOLILIME LOIPA	
-------------	-----------------------------------	--

10:6	madalitso	chiwawa
10:11		
10:14		
10:20		
10:21		
10:31		
10:32		
11:9		
11:11		
11:13		
12:6		
12:13		
12:17		
12:18		
12:19		
12:22		
13:3		
14:3		
14:5		
14:25		
15:2		
15:4		
15:7		
15:14		
15:28		
17:9		
19:1		

2. Mu Miyambo 6:16-19 muli zinthu zisanu ndi ziwiri zomwe Mulungu amadana nazo kwambiri. Kodi ndi zitatu ziti zomwe zimachitika ndi lilime?
3. Werengani mabuku a Masalimo ndi Miyambo ndipo muchite zinthu izi:

- A. Lembani mavesi onse omwe akulankhula za kugwiritsa ntchito lilime molakwika. Lembani mndandanda wanu molingana ndi ndondomeko ili m'musiyi:

VESI

Masalimo 5:9

Masalimo 10:7

(pitirizani mndandandawu)

KUGWIRITSA NTCHITO KOLAKWIKWA

Mau osyasyalika

Kutembelera ndi kunyenga

- B. Lembani mavesi ena owonetsa kagwiritsidwe ntchito koyenera. Alembeni mavesiwo molingana ndi dongosolo ili:

VESI

Masalimo 19:14

Masalimo 34:1

(pitirizani mndandandawu)

KUGWIRITSA NTCHITO KOYENERA

Mau ovomerezeka

Kudalitsa ndi kutamanda Mulungu kosalekeza

“Usabweretse umboni wabodza” (Eksodo 23:1). Mau oti “kubweretsa” mu vesi ili amatanthauza kulandira kapena kulankhula. Sitikuyenera kumvetsera kapena kufalitsa maumboni abodza. Afilipi 4:8 akutilimbikitsa kuti tizilingalira zabwino zokhazokha. Umu ndi momwe mungadziwire kuti munthu akukubweretserani umboni wabodza.

UMBONI WABODZA:

- Umayamba kufufuza za chikhalidwe ndi zolinga machitidwe a abale ndi alongo mwa Ambuye
- Umanyozza utsogoleri
- Umabweretsa kugawikana ndi mkwiyo. Ngati tikhala otanganidwa ndi kulimbana ndi wina ndi mnzake, sitingalimbane ndi mdani wathu, Satana, mwamphamvu.
- Umayang'ana zolephera zokhazokha.

UMBONI WABODZA UMACHOKERA KU ZOLINGA ZA:

- Matama: amadzikweza okha, nkumanyozza ena.
- Nsanje ndi kusilira: Munthuyo amasilira zomwe anzake ali nazo ndipo mwachinsinsi amawanyozza.
- Chikumbumtima: munthuyo amafuna kuti ena aoneke olakwa osati iyeyo.
- Kuukira: Mzimu woukira umalimbana ndi atsogoleri. Werengani nkhani ya Abisalomu m'Baibulo. (2 Samuel 15). Njira imodzi yodziwira kuti munthu ali ndi maganizo owukira amayamba ndi mau oti, “Ndikanakhala kuti mtsogoleri ndi ine ndikana...”
- Kuwawidwa mtima: Munthu amakhala kuti wavulazidwa, ndiye amafuna kuvulaza enanso ndi mau.

MUNGADZIWE BWANJI UMBONI WABODZA

- Munthuyo amakuyesani kaye. Atha kukufunsani kuti, “Kodi mumamva bwanji za.....?” Akufuna adziwe kaye maganizo anu asananene mabodza awowo.
- Munthuyo amakupangani kuti mukhale ndi chidwi. Atha kuyamba nkunena, “Simungakhulupirire zomwe ndamva.....” kapena “Kodi mwamva kuti.....?” Akufuna kudzutsa chidwi chanu kuti muwafunse zomwe akudziwazo.
- Amaoneka kuti akudziwa zinsinsi zina zake kapena ali ndi umboni weni weni. Ndiye amafuna kuti akukopeni kuti mukhale gulu la anthu ochepa omwe akudziwa zinsinsi zina zake.
- Amatha kuzidzimbaitsa ngati kuti akufuna uphungu wauzimu “Ndima funa nditadziwa maganizo anu pa,”, kenako nkupiriza ndi bodzalo mwauzimu.
- Atha kukuuzani ngati chopempherera. “Pakufunika tipempherere... chifukwa....” Kenako apiriza ndi miseche ya munthuyo.
- Atha kubwera ngati kuti akhuzika kwambiri ndi chinachake. “Koma zandikhuza bwanji....” Ichi chimakhala chiyambi cha mabodza omwe akubwera.

MOMWE MUNGALETSERE MABODZA

Mumfunse munthuyo mafunso awa:

- Chifukwa chiyani ukundiiza INE zimenezi?
- Inu mwazitenga kuti zimenezi – Nthawi anthu amabodza safuna kunena komwe amva nkhaniyo.
- Kodi munthuyo mwakumana naye kale molingana ndi zomwe ziri pa Mateyu 18:15-17?
- Kodi mwafufuza kuti ndi zoonā kapena mukungofalitsa zomwe mwamvazo?
- Kodi ndidzakutchuleni ndikapeza umboni weni weni wa nkhaniyi?
- Kodi mukuganiza kuti izi zikugwirizana ndi zomwe ziri pa Afilipo 4:8?

Kapena mutha kungomsula kuti, “Sindikufuna kumva zimenezi.”

CHAPUTALA 17

NKHONDO PA MALINGA

ZOLINGA

Mukamaliza phunziro lino mukhala mukukwanitsa kuchita izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
- Kufotokozero tanthauzo la “malinga auzimu”
- Kufotokozero chifukwa chomwe malinga awonongedwera.
- Kuzindikira machenjerero a Satana pogwetsa malinga auzimu.
- Kuzindikira njira zauzimu zotsutsira machenjerero kuti tikhale opambana pa nkondo ya pa malinga.

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Koma ndinawabwezera mau, ndi kunena nao, Mulungu Wam'mwamba, Iye ndiye adzatilemeza; cifukwa cace ife akapolo ace tidzanyamuka ndi kumanga; koma inu mulibe gawo, kapena ulamuliro, kapena cikumbukilo, m'Yerusalemu. (Nehemiya 2:20)

MAU OYAMBA

Bukhu la Nehemiya m'Chipangano Chakale ndi nkhani ya nkondo yomanganso malinga a Yerusalemu omwe anaonongeka ndi adani. Malinga anali odalirika ku chitetezo cha mizinda ya Israel wakale. Amateteza kwa adani obwera kudzathira nkondo mzinda. Malinga a kuthupi a Israel ndi fanizo la malinga athu auzimu:

Ciwawa sicidzamvekanso m'dziko mwako, kupululutsa pena kupasula m'malire ako; koma udzacha malinga ako Cipulumutso, ndi zipata zako Matamando. (Yesaya 60:18)

Zipata za Yerusalemu zomwe zatchulidwa pa Nehemiya 3 ziri ndi tanthauzo lauzimu chipata chilichonse pachokha.

Chipata cha Nkhosa chimailira ntchito ya mtanda m'moyo wanu, maziko a moyo wauzimu: 3:1; Yohane 10:11.

Chipata cha Nsomba chimatanthauza mboni ya Chikhristu: 3:3; Mateyu 4:19

Chipata Chakale chimaimilira kusinthika kwa moyo wakale kukhala watsopano: 3:13; Aroma 6:1-23

Chipata cha Chigwa chimalankhula za masautso and mayesero: 3:13; 2 Akorinto 1:3-5

Chipata cha Ndowe chimaimilira ntchito za thupi zomwe zikuyenera kuchotsedwa: 3:14; Agalatiya 5:16-21

Chipata cha Kasupe chimaimilira ntchito ya Mzimu Woyera: 3:15; Yohane 7:37-39

Chipata cha Madzi chimaimilira Mau a Mulungu 3:26; Yohane 4:10-14

Chipata cha Ngamira chimaimilira nkondo ya okhulupirira: 3:28; Aefeso 6:10-17.

Chipata cha Kummawa chimalankhula za chiyembekezo cha okhulupirira nkubwera kwa Yesu: 3:29; Ezekiel 43:1-2

Chipata cha Miphkadi chimakamba za kudziyesa wekha ndi mpando wa chiweruzo wa Yesu: 3:31; 1 Akorinto 3:9-15; 2 Akorinto 5:10.

Ndiye malinga anu auzimu muli:

- Malinga a chipulumutso, zipata za matamando
- Ntchito ya mtanda m'moyo wanu
- Umboni wa Chikristu
- Munthu wakale kusinthika kukhala watsopano
- Kusautsidwa ndi kuyesedwa
- Kuthana ndi ntchito za thupi
- Ntchito ya Mzimu Woyera
- Mau a Mulungu
- Nkhondo yauzimu
- Chiyembekezo cha kubweranso kwa Yesu
- Kudziyesa wekha

Awa ndi malinga omwe Satana amafuna atawaononga m'moyo mwanu. Akufuna aononge matamando ndi umboni wanu. Akufuna kuononga ntchito ya mtanda mwa inu, kusautsika komanso Mzimu Woyera m'moyo wanu. Amafuna kukuletsani kuti musawerenge Mau a Mulungu ndi kuwachita. Satana amafuna atakugonjetsani pa nkondo yauzimu, kukuletsani kuti musamadziyese nokha ndi kukukolani mu msampha ntchito za thupi ndi makhalidwe a munthu wakaleyo. Akufuna kuononga chiyembekezo chanu cha kubweranso kwa Yesu. Awa ndi malinga anu auzimu, Satana amafuna atawathira nkondo pogwiritsa ntchito njira zofanana ndi zomwe zinagwiritsidwa ntchito polimbana ndi malinga a Yerusalemu. Chaputala chino chikukamba za nkondo ya malinga a moyo wanu wauzimu. Tigwiritsa ntchito nkhani ya Nehemiya ndi kuonamo maphunziro ofanana ndi nkondo yauzimu.

ZOMWE ZIMACHITIKA MU YERUSALEMU

Tisanapirire ndi phunziro lino, werengani Nehemiya 1 mpaka 7:3. Ma chaputala 1 ndi 2 a Nehemiya akufotokozera za momwe malinga a Yerusalemu analiri. Anali bwinja ataonongedwa ndi adani obwera ndi nkondo, ndipo zipata zinaotchedwa ndi moto. Popanda malinga ndi zipata ndiye kuti mzinda unali wopanda chitetezo kwa mdani aliyense mbali zonse. Ngati malinga a moyo wanu wauzimu aonongedwa, inunso mulibe chitetezo popeza moyo wanu uli pa mbalambanda.

CHIYAMBI CHA VUTO

Nehemiya anadziwa kuti malinga aonongedwa ndipo mzinda wonse unali bwinja chifukwa cha uchimo (Nehemiya 1:5-7). Ngati malinga anu asanduka bwinja ndi chifukwa uchimo. Nehemiya anasowa mtendere ndi maitanidwe a Mulungu kuti akamange malinga a Yerusamu ndi kuteteza okhalamo. Dongosolo lake ndi kukonzekera kwake ziri mu chaputala 1 ndi 2. Iye ndi anyamata ake atsimikizika “kudzuka ndi kumanga” malinga (Nehemiya 2:18).

MACHENJERERO A SATANA NKHONDO YA PA MALINGA

Nehemiya atatsimikizika za kumanga linga kuzungulira Yerusalemu, anakumana ndi kutsutsidwa ndi adani ake. Mukatsimikizika za kumanga linga la moyo wanu, mukumananso ndi kutsutsidwa kuchokera kwa Satana, mdani wnau. Machenjerero a adani a Nehemiya ndi ofanana ndi machenjerero a mdierekezi pamene akulimbana ndi kumangidwa kwa linga la moyo wanu. Nkhondoyi yaikidwa m’magawo awiri: Nkhondo za kunjja ndi nkondo zamkati.

ZIWEMBU ZOCHOKERA KUNJA

Izi ndi ziwembu zimene Satana amagwiritsa ntchito anthu omwe sali mbali imodzi ya thupi la Khristu. Nkhondozi kapena ziwembuzi ndi monga:

1. Kunenedwa: Nehemiya 2:19
Adani anadzudzula Nehemiya, “Kodi ndiye chiyani mukuchitachi?” Anadana ndi ntchito yomanganso linga ndipo anayesetsa kutsekereza.
2. Kunyozedwa: Nehemiya 4:1-3
Nehemiya anali kunenedwa. Mdani anayesera kumgonjetsa kudzera m’malankhulidwe onyoza a anthu. Satana adzagwiritsa ntchito anthu kuti akugwetseni ulesi ndi kukugonjetsani.
3. Kumnenera zabodza: Nehemiya 6:5-7
Mdani anathira nkondo Nehemiya pamaso pomunenera zabodza. Anamnena kuti ndi woukira. Satana amatchedwa “woneneza abale.” Adzagwiritsa ntchito anthu ena kukunenerani zabodza komanso kuika zinthu zabodza m’maganizo mwanu.
4. Kupatutsa: Nehemiya 6:2

Adani anayesera kumuitana Nehemiya ku zokambirana ndi cholinga chakuti asiye ntchito yomanga malinga. Kupatutsidwa ku ntchito imene Mulungu wakupatsa nkumatanganika ndi zina ndi chenjerero lalikulu lomwe mdierekezi amagwiritsa ntchito.

5. Mphamvu zag ulu: Nehemiya 6:2

Mdani anati, “Tiyeni” tikumane pamodzi, ndi cholinga chompana Nehemiya kuganiza kuti pakuti ndi zag ulu ndipite nawo. Anthu omwewo anamunena kuti ndi woukira ndipo sangakwanitse kumanga malinga. Mdierekezi amafuna kusokoneza okhulupirira pa ntchito ya Mulungu poganiza kuti wina aliyense ali komweko, akuchita zomwezo, inenso. Iyi ndi njira yoopsa imene Satana akuigwiritsa ntchito lero. Mneneri wabodza wonena kuti watumidwa ndi Mulungu anagwiritsidwa ntchito pachiwembu chokonza Nehemiya (6:10-13). Maganizo a gulu atha kukhala oti “timvere zonena munthu wa Mulungu.” Baibulo likutichenjeza za aneneri onyenga omwe angatichotse pa ntchito ya utumiki.

6. Kunyengelera: Nehemiya 5:14-19

Nehemiya anakana kunyengerera. Sanalole kufanizidwa ndi moyo komanso makhalidwe omuzungulira. Mfundo yake inali yakuti, “Sindinatero ine, chifukwa cha kuopa Mulungu.” (Nehemiya 5:15). Satana amafuna anthu onyengelera ndi osatsimikizika pa chikhulupiriro chawo. Amafuna kuwanyenga kuti akukhulupirire kuti zinthuzo ndi zabwino popeza aliyense akuzimva kukoma kapena kuti sikuti ndi zolakwika kweni kweni?

7. Kuopsedwa ndi kuchita mantha: Nehemiya 6:5-9

Adani anachita zinthu zambiri zofuna kuopseza Nehemiya ndi anyamata ake ogwira nawo ntchito. Satana amadziwa kuti mantha amafooketsa koma chikhulupiriro chimapereka mphamvu kwa okhulupirira kuti atumikire Mulungu mwamphamvu. Nehemiya atapatsidwa mwayi woti athawe mdani, iye anakana kuthawa ndi kukweza manja (Nehemiya 6:10-13). Sanafune kupeza njira zachidule zothawira. Satana amayesetsa kuopseza okhulupirira kuti athawe akakumana ndi nyengo zowatsutsa. Pamene mukuthawa ndiye kuti mwakweza manja, ndipo ngati mwakweza manja mulibenso mphamvu zauzimu zoti muime. Ulendo wa chikhulupiriro ndi ulendo wa zowawa chifukwa cha iwo oyenda monga mwa thupi.

8. Kumenya nkhondo ndi kutsekereza: Nehemiya 4:8

Njira zomenya nkhondo ndi zotsekereza poyera zinagwiritsidwa ntchito. Satana sachita zinthu mobisala mokhamokha. Nthawi zina amabwera kumenyana nanu ndi kutsekereza ntchito ya Mulungu mwa inu poyera.

9. Maupo a chiwembu: Nehemiya 4:8; 6:2

Chiwembu chofuna kuthana ndi Nehemiya chinakonzedwa. Satana amachita maupo a chiwembu pa moyo wanunso:

Siibwera mbala koma kuti ikabe, kupha ndi kuononga.... (Yohane 10:10)

10. Ziwembu nthawi yoopsa kwambiri: Nehemiya 4:6

Satana anabwera ndi chiwembu choopsa kwambiri ntchito yomanga malinga itangofika theka popeza iyi inali nthawi yofunikira. Mdani amabwera ndi ziwembu nthawi imene inuyo muli opanda chitetezo kwenikweni.

- Mneneri Yona anali wokhumudwa kwambiri Ninevi atangolandira chitsitsimutso chachikulu (Yona 3-4)
- Davide anagwa mu uchimo nthawi yoti wagonjetsa adani ake onse pa moyo wake. Kufikira nthawi iyi, Davide anali asanagonjetsedweko ku nkondo.
- Samson anagwa mu uchimo “atangoyamba” kumasula Israel mu nsinga za Afilisti. Pamene mukuchita bwino kwambiri mu utumiki, mumatayilira pang’ono. Ndipo imeneyi imakhala nthawi yoopsa kwambiri. Satana amalimbana ndi iwo amene akuchita bwino mu dziko lauzimu.

ZIWEMBU ZOCHOKERA MKATI

Ziwembu za mkati ndi ziwembu zimene Satana amagwiritsa ntchito anthu ochokera mthupi la Khristu. Izi ndi monga:

1. Kufooketsedwa: Nehemiya: 4:10-11
Ogwira ntchito anali okhumudwitsidwa kwambiri zomwe zinapangitsa kutaika kwa:
 - Mphamvu
 - Masomphenya
 - Kulimbika mtima
2. Mikangano: Nehemiya 5.
Nehemiya 5 akuonetsera mikangano pakati pa anthu a Mulungu. Satana akagawa thupi la Khristu timakhala opanda mphamvu. Timakhala otanganidwa kulimbana wina ndi mnzake m’ malo mogwira ntchito. Magawano amabwera chifukwa cha kukhala ndi zolinga zolakwika. Mu Nehemiya 5 vuto lalikulu linali umbombo.
3. Okhulupirira ofowoka: Nehemiya 4:12
Mdani anagwiritsa ntchito ogwira ntchito ofowoka (chithunzithunzi cha abale mwa Ambuye olobodoka) kuti aimitse ntchito yomanga malinga.

NJIRA ZAUZIMU ZOTSUTSIRA MACHENJERERO CHIGONJETSO PA MALINGA

Nehemiya anagwiritsa ntchito njira zotsatirazi pomanganso malinga a Yerusalemu. Mutha kugwiritsa ntchito njira zomwezi kuti muone chipambano pa malinga anu auzimu.

FUFUZANI MALINGA

Monga momwe anachitira Nehemiya, mukuyenera kufufuza malinga a moyo wanu wauzimu (Nehemiya 2). Kodi mdani walowa m’ moyo wanu wauzimu, m’nyumba, mu mpingo kapena mu geni yanu?

Koma munthu adziyese yekha... (1 Akorinto 11:28).

Dziyese ni nokha ngati muli m'chikhulupiriro, dzitsimikizeni nokha... (2 Akorinto 13:5)

Kumbukirani kuti kudziyese nokha ndi chipata chimodzi muuzimu. Satana adzayeseza kukuletsani kuti musadziyese nokha chifukwa muzindikira madera amene mdani waononga linga lanu ndi kulowa.

VOMEREZEZANI TCHIMO LANU

Monga m'mene Nehemiya anazindikira kuti malinga aonongeka chifukwa cha uchimo (Nehemiya 1:5-7). Inunso vomerezani tchimo lanu ndi kulapa kupempha chikhululukiro:

Tikati kuti tiribe ucimo, tidziyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi. Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:8-9)

DZIWANI KUTI SIMUNGATHE KUMANGA NOKHA

Anyamata a Nehemiya m'mene amalankhula kuti, "Ife patokha sitingathe kumanga linga," amanena zoono. Paokha sakanatha kumanga. Amasowekera mphamvu ya Mulungu kuti iwapatse kuthekera kwa kugwira ntchitoyo. Inunso mukusowekera mphamvu ya Mulungu!

DZUKANI NDI KUMANGA

Monga ngati Nehemiya, tsimikizikani kudzuka ndi kumanga malinga a moyo wanu wauzimu:

Koma ndinawabwezera mau, ndi kunena nao, Mulungu Wam'mwamba, Iye ndiye adzatilemeza; cifukwa cace ife akapolo ace tidzanyamuka ndi kumanga; koma inu mulibe gawo, kapena ulamuliro, kapena cikumbukilo, m'Yerusalemu. (Nehemiya 2:20)

Khalani wokonzeka... Mukumana ndi zokulepheretsani za mdani.

MUSAPATUKE PA NTCHITO YOMANGA

Nehemiya anakana kupatutsidwa pa ntchito yomanga linga ndi machenjerero a adani (Nehemiya 6:2-3). Musamlole mdani akupatutseni pa ntchito yomanga linga lanu lauuzimu.

MUSATEKESEKE NDI ZOLANKHULA LANKHULA

Anthu ambiri anaona kuti Nehemiya ndi woukira (Nehemiya 2:19). Iwo amatsimikizika kuti linga la Yerusalemu silingamangidwenso molongosoka (4:3). Koma Nehemiya sanatekeseke ndi zolankhula anthu. M'malo mofooketsedwa ndi zolankhula za anthu, Nehemiya anakhala chitsanzo. “Inenso, chifukwa cha kuopa Mulungu (5:14-19). Khalani chitsanzo m'moyo wauzimu. Musakhale mbali imodzi ya zolankhula wanthu kuti chigonjetso nchosatheka.

MUDZIWENI MDANI NDI MACHENJERERO AKE

Nehemiya anamdziwa mdani ndi njira zake. Anatulukira kuti mdani amakonza zowathira nkhondo modzidzimutsa (4:8 ndi 11). Mukuyenera kumdziwa mdani wanu muuzimu ndi njira zake kuti mukachite bwino pa nkhondo yauzimu. Izi zikuthandizani kukhala wokonzeka ku nkhondo zothiridwa mwadzidzidzi. Dziwani kuti mdani akukonza chiwembu choti akupheni, kukubani ndi kukuonongani koma zindikirani kuti Mulungu ali ndi mphamvu zoposa ndipo akufuna kukupatsani moyo wochuruka (Yohane 10:10).

KONZANI NJIRA ZAUZIMU ZOTSUTSIRA MACHENJERERO

Nehemiya anakonzeratu njira zophelerera atangomva kuti mdani akukonza chiwembu. Anaika ogwira ntchito ena ngati alonda kukhala tcheru pamene mdani akubwera. M'misiri aliyense anali ndi lupanga - wokonzeka kumenya nkhondo mdani akabwera (Nehemiya 4:13-18). Anaikiratu chizindikiro (kuomba lipenga) kudziwitsa anthu za kubwera kwa adani. Popeza anali atadziwa njira za adani ndi kukonzekera, analetsa chiwembu chonse. Anali otsimikizika kuti ngati atabwera, Mulungu awamenyera nkhondo:

.... Mulungu wathu atimenyera nkhondo (Nehemiya 4:20).

Mukakhala ndi njira zabwino zauzimu zotsutsira mdani, mutha kukaniza ziwembu zambiri za mdani pa moyo wanu. Satana akaboola linga nalowa, tsimikizikani kuti Mulungu akumenyerani nkhondo.

KUMANA NAYENI MDANI MASO NDI MASO

Nehemiya atapatsidwa mwayi wopeza pothawira ndi adani, anakana. Iye anati, “Kodi munthu ngati ine nkuthawa?” (Nehemiya 6:11). Nehemiya anakumana ndi mdani mwa mphamvu ya Mulungu. Mdani akakuopsezani, musathawe kapena kupeza njira zachidule zodzitetezera popeza mukatero linga lauzimu la moyo wanu likhala pa chiopsezo. Pamene nkhondo zochokera mkati zinadzuka ndi kuti mdani anagwiritsa ntchito abale mwa Ambuye ofooka, Nehemiya sananyozere chiwembucho. Anakumana nawo adani nawagonjetsa.

TETEZANI LINGA LANU PA NTHAWI YOMWE LIRI PA CHIOPSEZO KWAMBIRI

Mu nkhani ya Nehemiya, chiwembu chachikulu cha mdani chinafika nthawi imene linga linali theka kuti limalizike. Mukayamba kumanga mu dziko lauzimu, mukalowa nthawi ya nkhondo

yowirikiza, khalani wokonzeka. Ndi nthawi yoopsa kwambiri. Satana akulunjikitsa ziwembu zake pa inu.

MANGANI MALINGA

Zomwe Nehemiya anachita atanyozedwa, kuneneredwa zoipa, kunamiziridwa, kuopsezidwa, ndi kuchita mantha kunali kupitirizabe kumanga.

Momwemo tinalikugwira nchito; gawo lina la iwo linagwira nthungo kuyambira mbanda kuca mpaka zaturuka nyenyezi. (Nehemiya 4:21)

Nehemiya anapirizabe ntchito. Sanasiye kumanga:

Ndipo linga linatsirizika pa tsiku la makumi awiri ndi lacisanu la mwezi wa Eluli, titalimanga masiku makumi asanu mphambu awiri. (Nehemiya 6:15)

Mu nthawi yochepa Nehemiya anakwanitsa kuchita zomwe adani amati sangathe kuchita.

Ngati malinga a moyo wanu ndi akugwa, mdani atha kukuuzani kuti nyengo yanu ndi yosatheka. Komano, ndi thandizo la Mulungu, mukhoza kumanga malinga anu. Ndi thandizo la Mulungu, sizifunikiranso nthawi yaitali kuti mukwaniritse.

Ndikhoza kuchita zonse kudzera mwa Khristu wondipatsa ine mphamvu (Afilipi 4:13).

Mdani akathira nkhondo ntchito yanu yauzimu yomanga, musaleke! Pitirizani kumanga malinga anu auzimu.

IKANI MLONDA

Nehemiya atatha kumanga malinga a Yerusalemu, anaika alonda kuti aziyang'anira malinga ndi zipata (Nehemiya 7:1-3). Ikani mlonda pa malinga anu auzimu. Khalani maso nthawi zonse ku ziwembu za mdani.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo

2. Kodi tanthauzo la malinga auzimu ndi chiyani?

3. Chifukwa cha chiyani malinga a Yerusalemu anaonongedwa (zifukwa chomwenso auzimu amaonongedwa)?

4. Lembani mndandanda wa njira zomwe Satana amagwiritsa ntchito pa nkhondo ya malinga auzimu.

5. Lembani mndandanda wa njira zauzimu zotsutsira machenjerero a Satana kuti tikapambane pa nkhondo ya malinga.

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto a bukhu lino).

MACHITACHITA A LUSO

1. Kodi pali malinga auzimu m'moyo wanu omwe aonongedwa ndi mdierekezi. Santhulani malinga anu auzimu monga:
 - Malinga a chipulumutso, zipata za matamando
 - Ntchito ya mtanda m'moyo wanu
 - Umboni wa Chikhristu
 - Munthu wakale kusinthika kukhala watsopano
 - Kusautsidwa ndi kuyesedwa
 - Kuthana ndi ntchito za thupi
 - Ntchito ya Mzimu Woyera
 - Mau a Mulungu
 - Nkhondo yauzimu
 - Chiyembekezo cha kubweranso kwa Yesu
 - Kudziyesa wekha
2. Okhulupirira amagonjetsedwa nthawi zambiri chifukwa chosowa kukonzekeretsedwa kwauzimu kokwanira. Werengani za momwe Nehemiya anadzikonzeretsera asanayambe kumanga malinga ndi kulimbana ndi adani.
 - Anaona momwe nyengo zinalili: Chaputala 1-2
 - Anazindikira tsinde la vuto kuti ndi tchimo ndipo analapa m'malo mwa iye yekha ndi anthu onse: Nehemiya 1:4
 - Anakonzekera mokwanira asanayambe kumanga ndi kukumana ndi mdani: Chaputala 1 ndi 2
 - Anakonza dongosolo la mamangidwe.
3. Kodi mwakonzeka kumanga malinga auzimu pa moyo wanu? Wonaninso zomwe mwaphunzira ndi kuzigwiritsa ntchito.

CHAPUTALA 18

NKHONDO ZA MADERA OFUNIKIRA

ZOLINGA:

Mukamaliza phunziro lino muzikwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kuzindikira machenjerero a Satana pa thupi lanu
- Kuzindikira njira zauzimu zotsutsira machenjerero a Satana kuti mukhale ndi chigonjetso pa thupi lanu
- Kufotokozera njira ya Satana yogwiritsa ntchito makhalidwe a munthu polimbana ndi okhulupirira
- Kulemba mwachidule njira zotsutsira machenjerero a mdierekezi makhalidwe a munthu kuti mupambane pa nkondo yolimbana ndi okhulupirira.
- Kuzindikira machenjerero a Satana polimbana ndi banja
- Kulemba mwachidule njira zotsutsira machenjerero pa chigonjetso cha nkondo ya banja
- Kuzindikira machenjerero a Satana pa nkhani ya ndalama ndi katundu.
- Kulemba mwachidule njira zotsutsira machenjerero a Satana pa chuma ndi katundu

VESI LOTSOGOLERA KUCHOKERA MU MFUNDO ZA NKHONDO

Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)

MAU OYAMBA

Ma chaputala a m'mbuyomu amakamba za ziwembu za mdani pa malingiliro, lilime, malinga anu auzimu komanso madera a nkondo monga dziko ndi thupi. Chaputala chino chikupitiriza kusanthula magawo apadera a ofunikira a thupi lanu, banja, ndalama omwe Satana amalunjika nkondo zake kudzera m'makhalidwe a munthu.

MACHENJERERO A SATANA ZIWEMBU ZAKUTHUPI

Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu? Ngati wina aononga kacisi wa Mulungu, ameneyo Mulungu adzamuononga; pakuti kacisi wa Mulungu ali wopatulika, ameneyo ndi inu. (1 Akorinto 3:16-17)

Chifukwa chakuti thupi lanu ndi kachisi wa Mzimu wa Mulungu, Satana adzalithira nkondo kudzera mu:

MATENDA

Matenda akupezeka pa dziko lapansi chifukwa cha tchimo loyamba la Adamu ndi Hava. Ngakhale izi ziri chomwechi, sizikutanthauza kuti aliyense yemwe akudwala ndi wochimwa.

Baibulo limafotokozera zifukwa zosiyanasiyana zomwe anthu amadwalira. Choyamba komanso chodziwikiratu ndi chakuti matenda amabwera ndi Satana. Satana amafuna kuzunza thupi momwe amachitira ndi moyo komanso mzimu kudzera mu kukhumudwitsidwa kapena kutsutsika. Sikuti thupi lanu lapulumuka ku ziwembuzi ayi. Koma matenda akhoza kugwiritsidwa ntchito ngati chikwapu kuthana ndi tchimo. Mwachitsanzo, onani nkhani ya Miriam mu Numeri 12.

Tsiku Yesu atachiritsa munthu anamuza kuti:

Zitapita izi Yesu anampeza m'Kacisi, nati kwa iye, Taona, waeiritsidwa; usacimwense, kuti cingakugwere ecipa coposa. (Yohane 5:14)

Ndi zotheka kuti munthu uyu amadwala chifukwa cha uchimo. Ndipo malo ena Yesu ananena poyera kuti matendawa si chifukwa cha uchimo koma kuti Mulungu akalemekezeke:

Ndipo popita, anaona munthu ali wosaona cibadwire. Ndipo akuphunzira ace anamfunsa iye, nanena, Rabi, anacimwa ndani, ameneyo, kapena atate wace ndi amace, kuti anabadwa wosaona? Yesu anayankha, Sanacimwa ameneyo, kapena atate wace ndi amace; koma kuti nchito za Mulungu zikaonetsedwe mwa iye.(Yohane 9:1-3)

Matenda obweretsa ulemelero kwa Mulungu ndi omwe Satana anabweretsa pa munthu koma ndi mphamvu yake wamchiritsa kudzera m'pemphepo kuti dzina lake likalemekezeke. Matenda a mtundu uwu ndi chiwembu cheni cheni chokokera kwa mdierekezi. Mukagwiritsa ntchito njira zotsutsira, chiwembu chakuthupichi chita kubweretsa ulemelero kwa Mulungu.

Si matenda onse omwe amabwera ndi Satana kapena tchimo kapena ngati chilango cha Mulungu. Matenda atha kubwera chifukwa cha kuchita zinthu mosemphana ndi chilengedwe cha Mulungu. Mwachitsanzo, matenda a kunyentchela thupi kapena kuthyola mwendo mutadumphika kuchoka pamwamba kwambiri. Satana amatha kumpanga munthu kuchita zinthu zosemphana ndi malamulo a chilengedwe kuti mupeze vuto pa thupi panu. Atha kukupangani kukupangani kusadya ndi kusamalira thupi lanu moyenera popeza amadziwa kuti mukatero mutha kudwala ndi cholinga chakuti musamtumikire Mulungu mwamphamvu.

KUTOPA KOPYOLA MUYEZO

Chifukwa cha kugwira ntchito yolemetsa nthawi yaitali kapena kukhala wotanganidwa nthawi zonse, thupi limafika pomva kutopa kopyola muyezo. Mukatopa kwambiri, Satana amapezerapo

mwayi wokuthirani nkondo. Satana anabwera kwa Yesu kudzamuyesa nthawi yoti anali wotopa kwambiri chifukwa cha kusala kudya kwa masiku makumi anayi (Mateyu 4:2). Eliya anali wokhumudwa kwambiri nafuna kufa atangochita kumene chozizwa chachikulu koopsa (1 Mafumu 19:4).

IMFA

Ngakhale imfa idzafikira munthu aliyense kufikira Yesu adzadza, Satana amatha kubweretsa imfa za msangamsanga. Amatha kupangitsa munthu kudzipha yekha. Atha kukupangani inu kuchita mantha kwambiri ndi matenda kapena ngozi mpakana kumwalira.

KUZUNZA THUPI

Satana amapangitsanso anthu kuika mthupi mwao mankwala owopsa monga ozunguza bongo kapena mowa. Amadziwa kuti zimenezi zitha kuyambitsa matenda mthupi, misala komanso imfa.

NJIRA ZA UZIMU ZOTSUTSIRA MACHENJERERO CHIGONJETSO PA ZIWEMBU ZA PATHUPI

Ngati mwadwala, pempherani kuti mudziwe chomwe chayambitsa matendawo. Kodi mwaphwanya lamulo la chilengedwe? Mwina kudya mosayenera kapenanso kumwa madzi oipa? Mwachitsanzo, kusuta fodya kumatha kuyambitsa chifuwa chachikulu pamene utsi umakaononga mapapo.

Ngati mwaphwanya lamulo la chilengedwe, Mulungu atha kukuchiritsanibe. Koma mukuyenera kugwiritsa nthcio nzeru mtsogolomu. Kumbukirani kuti thupi lanu ndi kachisi wa Mulungu. Pewani kuphwanya malamulo a chilengedwe ndi kuyamba kusamalira bwino thupi lanu. Izi ndi zofunika kukumbukira ngakhale pa nkhani ya kutopa kowirikiza. Yesu anaitana ophunzira ake akapumule pamene anali wotopa chifukwa cha kutumukira kwambiri (Marko 6:31).

Pamene Eliya anatopa ndi kukumudwa, anapumula pansu pa mtengo ndipo Mulungu anatumiza mngelo ndi chakudya chakuthupi. Iye anadikira kukudza kwatsopano kuchokera kwa Mulungu ndipo mphamvu zake zinapangidwa kukhalanso zatsopano kukonzekera mavuto a utumiki wina (1 Mafumu 19:4-8).

Matenda akabwera ngati mbali imodzi ya chilango cha Mulungu pa inu, osati chifukwa cha mphamvu zakumdima, kumanga ziwanda sikuphula kanthu. Kulapa ndi kubwerera kwa Mulungu kokha basi ndi komwe kungakonze zinthu ndi kubweretsa ufulu.

**Tiyeni, tibwerere kunka kwa Yehova; pakuti wang'amba, nadzatipoletsera;
wakantha, nadzatimanga. (Hosea 6:1)**

Pakuti ndidzakubwezera iwe moyo, ndipo ndidzapoletsa mabala ako, ati Yehova; cifukwa anacha iwe wopitikitsidwa, nati, Ndiye Ziyoni, amene kulibe munthu amfuna. (Yeremiya 30:17)

ndipo anati, Ngati udzamveratu mau a Yehova, Mulungu wako, ndi kucita zoonza pamaso pace, ndi kuchera khutu pa malamulo ace, ndi kusunga malemba ace onse, za nthenda zonse ndinaziika pa Aaigupto sindidzaziika pa iwe nnena imodzi; pakuti Ine Yehova ndine wakuciritsa iwe. (Eksodo 15:26)

Amene akhululukira mphulupulu zako zonse; Naciritsa nthenda zako zonse; (Masalimo 103:3)

Ngati okhulupirira, tikuyenera kukumbukira nthawi zonse kuti ngakhale Satana achite ziwembu za mtundu wanji, koma Mulungu akutetezera moyo wanu. Satana sangakhudze thupi lanu kapena kuchotsa moyo wanu Mulungu osadziwa. Werengani Yobu 1 ndi 2 muona kuti akuchitira umboni za ichi. Mphamvu ya Mulungu imaposa ya mdierekezi. Mulungu amene analenga thupi ali ndi mphamvu ya kuchiritsa thupilo. Mukakumana ndi ziwembu za pa thupi panu, lengezani za kukwaniritsidwa kwa malonjezano awa:

Ndipo ndinatama akufa atatha kufa kupambana amoyo omwe alipobe; (Mlaliki 4:2)

Amene anasenza macimo athu mwini yekha m'thupi mwace pamtanda, kuti ife, 7 titafa kumacimo, tikakhale ndi moyo kutsata cilungamo; 8 ameneyo mikwingwirima yace munaciritsidwa nayo. (1 Petro 2:24)

Koma Iye analasidwa cifukwa ca zolakwa zathu, natundudwidwa cifukwa ca mphulupulu zathu; cilango cotitengera ife mtendere cinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yace ife taciritsidwa. (Yesaya 53:5)

cifukwa ca coonadi cimene cikhala mwa ife, ndipo cidzakhala ndi ife ku nthawi yosatha: (2 Yohane 1:2)

Satana akakuthira nkondo thupi lanu, itanitsani mapemphero a okhulupirira ena, kuphatikizapo akulu ampingo pamodzi ndi iwo amene ali ndi mphatso ya machiritso:

kwa wina cikhulupiriro, mwa Mzimu yemweyo; ndi kwa wina mphatso za maciritso, mwa Mzimu mmodziyo; (1 Akorinto 12:9)

Ndipotu Mulungu anaika ena m'Eklesia, poyamba atumwi, aciwiri aneneri, acitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso zamaciritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu. (1 Akorinto 12:28)

Pali wina kodi adwala mwa inu? Adziitanire akuru a Mpingo, ndipo apemphere pa iye, atamdzoza ndi mafuta m'dzina la Ambuye: ndipo pemphero la cikhulupiriro lidzapulumutsa wodwalayo, ndipo Ambuye adzamuukitsa; ndipo ngati adacita macimo adzakhululukidwa kwa iye. (Yakobo 5:14-15)

Kumwalira m'thupi ndi mbali imodzi ya moyo uno kufikira nthawi ya chimaliziro monga timadziwira. Okhulupirira sakuyenera kuopa imfa popeza tili ndi lonjezano la moyo wosatha:

koma tilimbika mtima, ndipo tikondwera makamaka kusakhala m'thupi, ndi kukhala kwathu kwa Ambuye. (2 Akorinto 5:8)

Satana sangachotse moyo wa wokhulupirira nthawi ya imfa yake isanafike, monga tikuonera nkhani ya Yobu. Mulungu sachita zinthu motsutsana ndi zisankho za anthu. Ngati munthu wayesedwa ndi mdierekezi kuti adziphe, mwachitsanzo, ndipo iye ndi kugonjera ku yeserolo, Mulungu saletsa ntchito ya chifuniro cha munthuyo.

MACHENJERERO A SATANA ZIWEMBU ZA PA CHIKHALIDWE CHA MUNTHU

Njira ina imene Satana amagwiritsa pobweretsa ziwembu pa inu ndi kudzera mu zikhalidwe za anthu. Satana atha kugwiritsa ntchito anthu omwe akuzungulirani kukuthirani nkondo yauzimu. Chiwembucho kutha kubwera kudzera mwa achibale, amnzanu, mpingo, adani, anthu ochita nawo malonda, ngakhale anthu achilendo kumene. Makhaliidwe amenewa amatha kudzimbaitidwa ngati “mngelo wa kuunika,” atumwi, ndi atumiki a chilungamo. Koma amakhala kuti Satana akugwira ntchito mkati mwao:

Pakuti otere ali atumwi onyenga, ocita ocenjerera, odzionetsa ngati atumwi a Kristu, Ndipo kulibe kudabwa; pakuti Satana yemwe adzionetsa ngati mngelo wa kuunika. Cifukwa cace sikuli kanthu kwakukuru ngatinso atumiki ace adzionetsa monga atumiki a chilungamo; amene cimaziro cao cidzakhala monga nchito zao. Ndinenanso, Munthu asandiyese wopanda nzeru; koma ngati mutero, mundilandirensa ine monga wopanda nzeru, kuti inenso ndidzitamandire pang'ono. (2 Akorinto 11:13-16).

Njira ya kugawira mizimu ifotokozeredwa bwino patsogolopa. Koma Satana alinso ndi njira zina zogwiritsira ntchito makhaliidwe a munthu. Iye akhoza kugwiritsa ntchito anthu ena kuti akupatseni uphungu woipa. Werengani bukhu la Yobu ndiye muone uphungu umene Yobu amalandira kuchokera kwa anzake komanso mkazi wake. Uneneri ndi mphatso ya Mzimu Woyera, koma Satana naye ali ndi aneneri ake. Mauneneri a pa munthu odzera mu chikhalidwe cha munthu sakhala ochokera kwa Mulungu nthawi zonse. Werengani za nkhani ya ngati iyi mu 1 Mafumu 13. Ziwembu za Satana nthawi zina zimadzera kwa abwenzi odalirika, adani komanso anthu osatembenuka mtima:

Pakuti si mdani amene ananditonzayo; Pakadatero ndikadacilola: Amene anadzikuza pa ine sindiye munthu wondida; Pakadatero ndikadambisalira: Koma ameneyo ndiwe, munthu woyenerana nane, Tsamwali wanga, wodziwana nane. Tinapangirana upo wokoma, Tinaperekeza khamu la anthu popita ku nyumba ya Mulungu.(Masalimo 55:12-14)

Satana amagwiritsanso ntchito makhalidwe a munthu kumpanga kukhumba kutenga ulemelero wa Mulungu pa iye:

Ndipo anthu osonkhanidwawo anapfuula, Ndiwo mau a Mulungu, si a munthu ai. Ndipo pomwepo mngelo wa Ambuye anamkantha, cifukwa sanampatsa Mulungu ulemerero; ndipo anadyedwa ndi mphutsi, natsirizika. (Machitidwe 12:22-23).

Satana amagwiritsa ntchito anthu kuti akuchotseni pa dongosolo lake la Mulungu m'moyo wanu. Werengani za momwe Petro anagwiritsidwira ntchito ndi Satana kummukira Yesu mu njira imeneyi (Marko 8:31-33). Iye akhoza kukupangani maso anu akhale pa munthu wina osati pa inu. Petro anasiya kuona za dongosolo la Mulungu pa moyo wake nachita chidwi ndi maitanidwe a Yohane (Yohane 21:31-33).

Satana adzakuyesani kuti “mutengere” yomwe ndi ntchito ya thupi (Agalatiya 5:19-21). Kufuna kukhala ngati munthu wina yemwe mumamsilira ndi njira imodzi ya Satana. Pamene mukulimbana ndi maitanidwe a wina mumakhala mukuchoka pa dongosolo la maitanidwe a Mulungu pa moyo wanu. Satana amagwiritsa ntchito anthu kuti akunyengeni. Werengani za momwe zinakhala ndi Yoswa (Yoshua 9). Anthu adzakusiyani (2 Akorinto 4:16-17); Machitidwe 15:37-38; Yohane 6:66). Satana adzayesetsa kutsekereza zolinga za utumiki wanu pa anthu ena (1 Atesalonika 2:18), ndipo adzabweretsa chisokonezo ndi kusagwirizana (1 Akorinto 14:33; Yakobo 3:26). Iye adzayesetsanso kugwiritsa ntchito anthu ena azisokoneza zolinga zanu. Werengani momwe zinachitkira ndi Yoseph mu Genesisi 37 ndi 39.

NJIRA ZAUZIMU ZOTSUTSIRA MACHENJERERO KUPAMBANA NKHONDO PA MAKHALIDWE A MUNTHU

Mu chaputala chikubwerachi cha kugawira mizimu muphunzira za kufunika kosankha bwino abwenzi. Iyi ndi njira yabwino yogonjetsera machenjerero a Satana pakupambana nkondo ya ziwembu zodzera kwa ena. Kusankha bwino abwenzi kudzachotsa chinyengo chachikulu, kusokonezeka, mikangano, komanso kutsekerezeka kwa moyo wauzimu.

Njira ziwiri zotsutsira machenjerero pa nkondo ya makhalidwe a anthu zomwe ndi zofunikiranso kwambiri.

Poyamba: Mverani Mulungu osati munthu.

Ndipo anayankha Petro ndi atumwi, nati, Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu. (Machitidwe 5:29)

Kachiwiri: Tsatirani za okhawo omwe akutsatira Mulungu.

Khalani onditsanza ine, monga inenso oditsanza Kristu. (1 Akorinto 11:1)

Cifukwa cace khalani akutsanza a Mulungu, monga ana okonedwa; (Aefeso 5:1)

Musalandire uneneri kapena uphungu kuchokera kwa munthu aliyense ngati zikusemphana ndi choonadi cha Mau a Mulungu. Musasilire kapena kutsatira anthu omwe moyo wao sulingana ndi Mau a Mulungu. Dziwani kuti mudzapambana pokhapokha ngati mutsatira dongosolo la Mulungu pa moyo wanu. Simungapambane ngati muzingotsatira za anthu ena. Musasokoretsedwe ndi iwo akukuzungulirani. Dalirani bvumbulutso la Mulungu osati zochita anthu.

Ngakhale kuti anthu okuzungulirani atha kusokoneza zinthu zina m'moyo wanu, kumbukirani kuti Mulungu ndiye wolamulira zinthu m'moyo mwanu. Ngakhale Yosefe anakumana ndi zovuta chifukwa cha machitidwe a anthu, Mulungu anasintha zovutazo kukhala zabwino:

Ndipo tsopano sindinu amene munanditumiza ine ndifike kuno, koma Mulungu, ndipo anandiyesa ine atate wa Farao, ndi mwini banja lace lonse, ndi wolamulira dziko lonse la Aigupto. (Genesisi 45:8)

Koma inu, munandipangira ine coipa; koma Mulungu anacipangira cabwino, kuti kucitike monga lero, kupulumutsa amoyo anthu ambiri, (Genesesi 50:20)

MACHENJERERO A SATANA NKHONDO YA PA BANJA

Banja ndi gawo laling'ono la mudzi lokhazikitsidwa ndi Mulungu pamene analenga munthu ndipo liri pa mtima wa Mulungu. Anadzutsa mtundu wa anthu osankhika kuchokera m'banja la munthu m'modzi, Abraham. Anasankha ubale wa pakati pa mamuna ndi mkazi pofotokozera za ubale wauzimu pakati pa Khristu ndi mpingo. M'Baibulo lonse, Mulungu amatsindika za kufunika kwa banja mu dongosolo lake lonse la mibadwo.

Banja ndi tsinde la maudindo ndi maulamuliro onse. Atsogoleri a boma ndi mpingo amakulira m'banja. Dera kapena dziko limakhala kuti liri ndi mabanja ambiri omwe ali pamodzi. Chifukwa cha kufunikira kwa gawo limeneli, Satana amathira nkhondo mabanja nthawi ndi nthawi.

Iye amasokoneza ubale wa mwamuna ndi mkazi wake. Amabweretsa chimpwirikiti cha maubale ogonana omwe amapititsa patsogolo uchimo (1 Akorinto 7:5). Amatsogoloera azibambo ndi

azimayi ku chigololo (Agalatiya 5:19). Amatha kupangitsa munthu m' modzi m' banja kuti asokoneze mzake kunchotsa pamaso pa Mulungu (Yobu 2). Satana amabweretsa kugawikana mnyumba kuyambira pa mikangano kukathera ku kusiyana kwa banja. Iye amayesetsa kubweretsa magawano chifukwa amadziwa kuti:

Ndipo Yesu anadziwa maganizo ao, nati kwa iwo, Ufumu uti wonse wogawanika pa wokha sukhalira kupasuka, ndi mudzi uti wonse kapena banja logawanika pa lokha silidzakhala; (Mateyu 12:25)

Ngati Satana angabweretse magawano ndi kuononga mabanja a dziko, ndiye kuti dzikolo wathana nalo.

Mulungu anakhazikitsa dongosolo la makhalidwe a m' banja. Mwamuna ndiye mutu wa banja ndipo akuyenera kukonda mkazi wake. Mkazi agonjere ku utsogoleri wake ndipo ana onse akhale omvera makolo awo (1 Akorinto 7; Aefeso 5:1-6:1). Satana amasokoneza mwamuna kuti asamachite zinthu zoyenera m' banja. Izi zimapangitsa kuti mkazi ndi ana asamamvere. Ndipo amatha kusokonezanso mkazi kuti aziukira ndi kusamvera mwamuna wake. Satana amasokoneza ngakhale ana mnyumba. Amatha kubweretsa kusaweruzika mwa ana ndi cholinga choika banjalo pa moto chifukwa cha makhalidwe a ana. Werengani nkhani ya pa 1 Samuel 2 ndi ya mwana wa Davide, Abisalomu, mu 2 Samuel 13-19.

Yesu anachenjeza za nkondo ya Satana m' nyumba zathu:

pakuti kuyambira tsopano adzakhala m'nyumba imodzi anthu asanu, atatu adzatsutsana ndi awiri, ndi awiri adzatsutsana ndi atatu. Adzatsutsana atate ndi mwana wace, ndi mwana ndi atate wace; amace adzatsutsana ndi mwana wamkazi'l ndi mwana wamkazi ndi amace, mpongozi adzatsutsana ndi mkazi wa mwana wace, ndi mkaziyo ndi mpongozi wace. (Luka 12:52-53)

NJIRA ZOTSUTSIRA MACHENJERERO CHIGONJETSO PA BANJA

Mavuto ambiri m' banja atha kupewedwa ngati munthu atasankha moyenera mnzake wa banja. Baibulo limachenjeza kuti munthu wotembenuka mtima asakwatirane ndi munthu wosatembenuka mtima:

Kodi awiri adzayenda pamodzi asanapanganiranetu? (Amosi 3:3)

Musakhale omangidwa m'goli ndi osakhulupira osiyana; pakuti cilungamo cigawanabwanji ndi cosalungama? Kapena kuunika kuyanjana bwanji nw mdima? (2 Akorinto 6:14)

Banja likakhala kuti wina ndi wokhulupirira ndipo wina ndi wosakhulupirira, magawano auzimu ayambika kale. Kugawikana uku sikulimbana kwa thupi ndi mwazi. Ndi nkondo yauzimu. Simungapambane ndi mau okwiya kapena kukangana ndi kutsutsana.

Satana amalimbana ndi umodzi wa banja chifukwa umaimilira umodzi wa Khristu ndi mpingo. Okhulupirira akuyenera kuzindikira ichi ndi kulengeza:

.... koma ine ndi a pabanja langa, tidzatumikira Yehova (Yoswa 24:15)

Ngati wolowa mnyumba wa lonjezano la Abraham, mutha kulengeza lonjezano lakuti, “Mwa iwe mabanja onse a dziko lapansi adzadalitsika” (Genesesi 12:3). Popeza kuti ndinu wolowa mnyumba wauzimu wa lonjezano la Abrahamu, banja lanu lidzadalitsika.

Kuti banja litetezeke ku machenjerero a mdierekezi, banjalo likuyenera kukula pamodzi muuzimu. Pemphero ndi kusanthula Mau pamodzi kumamangilira mabanja:

Ndipo mau awa ndikuuzanilero, azikhala pantima panu; ndipo muziwaphunzitsa mwacangu kwa ana anu, ndi kuwalankhula awa pokhala pansu m'nyumba zanu, ndi poyenda inu panjira, ndi pogona inu pansu, ndi pouka inu. Ndipo muziwamanga padzanja panu ngati cizindikilo, ndipo akhale ngati capamphumi pakati pa maso anu. Ndipo muziwalemba pa mphuthu za nyumba zanu, ndi pa zipata zanu. (Deuteronomu 6:6-9)

Munthu asakhale mdindo mu mpingo, banja lake likuyenera likhale lolongosoka. Chipangano Chatsopano chimafuna otsogolera akhale ndi nyumba zolongosoka. (Onani Tito 1 ndi 1 Timoteyo 3). Anthu ambiri podzipereka ku utumiki mowirikiza aika mabanja awo pa moto. Kuti mugonjetse machenjerero a Satana m'gawo limeneli, banja lanu likhale molingana ndi dongosolo la Mulungu musanatenge mpando uliwonse wautsogoleri mu mpingo.

Makolo ali ndi udindo wolanga ana awo kuti akhale ndi chikhalidwe chabwino. Mavuto a m'banja la Eli ndi Davide anabwera chifukwa chosaphunzitsa ana chikhalidwe chabwino. Baibulo likulangiza okhulupirira pa udindo umenewu:

Phunzitsa mwana poyamba njira yace; Ndipo angakhale atakalamba sadzacokamo. (Miyambo 22:6)

Wolekereramwanace osammenya amuda; Koma womkonda amyambize kumlanga. (Miyambo 13:24)

**MACHENJERERO A SATANA
NKHONDO YA ZACHUMA**

Dera lina limene Satana amalimbana nalo m'moyo wa okhulupirira ndi gawo la ndalama ndi zachuma. Nkhondo zake ziri m'magawo awiri:

Gawo loyamba: Kusokonezeka kwa chuma ndi ndalama za wokhulupirira popanda vuto lina liri lonse. Ichi ndi chiwembu cha mdierekezi pa okhulupirira.

Gawo lachiwiri: Kusokonezeka kwa chuma ndi ndalama za okhulupirira chifukwa chosayenda m'Mau.

Chitsanzo chabwino pa chiwembu choyambachi ndi nkhani ya Yobu mu chaputala 1 ndi 2. Satana anathira nkhondo chuma cha Yobu powononga ziweto zake ndi nyumba yake. Denga kuloshokera mkati. Baibulo limanena kuti Yobu anali munthu wolungama ndiye kuti palibe lembe lirilonse limene iye anaphwanya.

Gawo lachiwiri la chiwembu cha mdierekezi ndi lophwanya malamulo a Mulungu. Satana amadziwa kuti akapangitsa anthu kuphwanya malemba, ndiye kuti ngakhale chuma chawo sichiyenda bwino. Amadziwa kuti popanda chuma ndi ndalama kutumikira Uthenga Wabwino pa dziko lonse lapansi sikuchitika mwamphamvu.

Werengani mavesi ali m'musiwa muone momwe Satana amathirira nkhondo chuma chatu:

- Kukhala pa ubale wa malonda ndi anthu osakhulupirira: 2 Akorinto 6:14-18. (Vesi ili timagwiritsa ntchito pa nkhani za mabanja okha. Koma likuyenera kugwiritsidwa ntchito pa maubale onse a pakati pa okhulupirira ndi osakhulupirira).
- Ngongole: Aroma 13:8
- Kuchitira umboni ngongole za anthu ena: Miyambo 6:1-2
- Kusalipira antchito koma ndalama zilipo: Miyambo 3:27-28
- Kusapereka chakhumi ndi zopereka: Malaki 3:1-12; Miyambo 11:24
- Kusowa chilungamo: Miyambo 16:8; Machitidwe 5:3-4
- Katangale: Yakobo 5:3-4
- Malipiro osayenera: Yereimiya 22:13
- Umbombo: Miyambo 28:22
- Kudya ndalama mosakaza: Miyambo 23:21
- Kuzemba misonkho ya boma: Aroma 13:6-7
- Ulesi womwe umabweretsa umphawi: Miyambo 20:13
- Kutsata njira zoipa kuti mulemere msanga: Miyambo 20:21; 28:22
- Chikondi cha pa ndalama: 1 Timoteyo 6:10
- Malonda ndi chuma zolemetsa: 2 Timoteyo 2:4
- Kupeputsa nkhani ya chopereka komanso kulandira mathandizo mosayenera kuti ulemere: 1 Samuel 2:29
-

NJIRA ZAUZIMU ZOTSUTSIRA MACHENJERERO

CHIGONJETSO PA NDALAMA NDI CHUMA

Satana akhoza kuononga chuma ndi katundu wa okhulupirira popanda cholakwa china chirichonse. Mwaona kale nkhani ya Yobu. Komano kumbukirani kuti Satana sanakhudze zinthu za Yobu popanda chilolezo chochokera kwa Mulungu. Ichi chinali chiwembu chakuti Mulungu anachivomereza ndicholinga chakuti akayese chikhulupiriro chake. Popeza Yobu anakhalabe wokhulupirika, Mulungu anamudalitsa kowirikiza kuposa m'mene analili poyamba.

Mukakumana ndi mavuto a zachuma popanda vuto kapena tchimo liri lonse, dziwani kuti ndi chiwembu cha Satana mdierekezi. Koma ngati mukhalabe wokhulupirika nimupitiriza kutsata malamulo a Mulungu pa kayendetsedwe ka chuma chanu, dalitso la Mulungu la kubwezeretsa litsatira yeserolo lomwe ndi la kanthawi:

Ndipo Yehova anadalitsa citsiriziro ca Yobu koposa ciyambi cace, ndipo anali nazo nkhosha zikwi khumi ndi zinai, ndi ngamila zikwi zisanu ndi cimodzi, ndi ng'ombe zamagoli cikwi cimodzi, ndi aburu akazi cikwi cimodzi. (Yobu 42:12)

Ngati mukukumana ndi mavuto a zachuma chifukwa cha kuphwanya malamulo a Mulungu, lapani ndikukonza zinthu. Thetsani maubale a malonda ndi anthu osakhulupirira (2 Akorinto 6:14-18). Siyani kukhala wopanda chilungamo (Miyambo 16:8; Machitidwe 5:3-4) ndi kusiya kuzemba misonkho ya boma (Aroma 13:6-7). Kutu muthane ndi nkondo za mdierekezi pa chuma chanu, musiyeye katangale (Yakobo 5:3-4) komanso malipiro a chinyengo (Yeremiya 22:13). Muleke umbombo (Miyambo 28:22) kusakaza ndalama (Miyambo 23:21), ndi ulesi (Miyambo 20:13).

Mupewe kuchita mtundu wa malonda omwe angakupangitseni kukhala wopanda mphamvu pakumenya nkondo yauzimu (2 Timoteyo 2:4). Mukane kutsata njira zachidule kuti mulemere msanga (Miyambo 20:21; 28:22) zomwe zimabwera chifukwa cha chikondi cha pa ndalama (1 Timoteyo 6:10). Dalirani Mulungu osati chuma chanucho (Deuteronomu 8:18-19; Masalimo 49:6). Musalole kuchitira umboni munthu wina kutenga ngongole (Miyambo 6:1-2) ndipo mutuluke m'moyo wa ngongole (Aroma 13:8; Miyambo 3:27-28).

Ngati simupereka chakhumi ndi zopereka, yambani kutero (Miyambo 11:24; Malaki 3:1-12). Mwina muli pa udindo wakuti mumalandira thandizo la chuma, siyani kugwiritsa ntchito pa zofuna zanu kapena kupeputsa chopereka (1 Samuel 2:29). Mukamapereka kwa Mulungu perekani chopereka ndi chakumi:

- Mwakufuna mtima wanu: Eksodo 35:5; 1 Mbiri 29:9
- Ndi mtima wolungama: 1 Mbiri 29:9
- Momasuka: Mateyu 6:38
- Mwachinsinsi: Mateyu 6:3
- Pafupi pafupi: 1 Akorinto 9:7

- Modzichepetsa: Aroma 12:8
- Molingana ndi kupeza kwanu: Mateyu 5:42
- Molingana ndi kuthekera kwanu: Ezra 2:69
- Mwa muyeso wa zomwe mwapeza: Genesesi 14:20; 28:22; Levitiko 27:30; 2 Mbiri 31:5; Malaki 3:10.

Ndi pokhapokha mwathana ndi kusayeruzika uku kuti mukangonjetsa machenjerero a Satana mu dera la za chuma.

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera mu Mfundo za Nkhondo

2. Lembani ziwembu zina za Satana pa thupi la munthu.

3. Lembani mwachidule njira zotsutsira ziwembu za Satana pa thupi la munthu.

4. Kodi Satana amagwiritsa ntchito motani makhalidwe a anthu polimbana ndi okhulupirira?

5. Lembani njira zina zotsutsira ziwembu za mdierekezi pa chigonjetso cha pa chikhalidwe cha anthu kulimbana ndi okhulupirira.

6. Kodi njira zina zomwe Satana amagwiritsa ntchito polimbana ndi mabanja ndi ziti?

7. Lembani njira zina zotsutsira ziwembu za mdierekezi pa mabanja.

8. Kodi ndi machenjerero ati a mdierekezi mu gawo la zachuma?

9. Lembani njira zina zotsutsira mdierekezi pa chigonjetso cha pa zachuma ndi ndalama.

(Mayankho a mafunso awa ali kumapeto kwa bukhu lino)

MACHITA CHITA A LUSO

Werengani bukhu la Yobu. Yobu anachitidwa chiwembu m' magawo a thupi, banja, chuma ndi makhalidwe a anthu. Kuseli kwa ziwembu zonsezi ndi magawo onsewa kunali chifukwa chazimu. Onani Yobu 1:6-12; 2:1-6; 42:5.

KUMBUKIRANI: Kuseri kwa chochitika kapena vuto liri lonse lomwe kukumana nalo kuli chifukwa chazimu.

Kuti mudziwe zambiri za matenda ndi kuchiritsidwa kwa thupi lanu ndi Mulungu, pezani phunziro la “Nkhondo Yathupi” la Harvestime Internationala Institute. Chifukwa cha chimenechi, sitinabwereze kukamba za machiritso auzimu athupi. Nkofunika kusanthula zambiri za dera limeneli popeza ndi gawo lalikuru limene Satana amagwiritsa ntchito polimbana ndi thupi lanu.

Kodi mukulimbana ndi nkhondo za thupi ndi chuma? Kodi kaperekedwe kanu kakugwirizana ndi zomwe mwaphunzira m'phunziro lino? Kodi mumapereka:

- Mwakufuna mtima wanu: Eksodo 35:5; 1 Mbiri 29:9
- Ndi mtima wolungama: 1 Mbiri 29:9
- Momasuka: Mateyu 6:38
- Mwachinsinsi: Mateyu 6:3
- Pafupi pafupi: 1 Akorinto 9:7
- Mokondwera: 2 Akorinto 9:7
- Modzichepetsa: Aroma 12:8
- Molingana ndi kupeza kwanu: Mateyu 5:42
- Molingana ndi kuthekera kwanu: Ezra 2:69
- Mwa muyeso wa zomwe mwapeza: Genesesi 14:20; 28:22; Levitiko 27:30; 2 Mbiri 31:5; Malaki 3:10.

CHAPUTALA 19

KUPATSIRANA MIZUMU

ZOLINGA

pamapeto pamaphunziro awa muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- kufotokozera tanthauzo la kupatsiraana mizimu
- kupereka chitsanzo cha m’Baibulo chopatsirana mzimu wabwino.
- kupereka chitsanzo cha m’Baibulo chopatsirana mzimu oipa.
- kufotokozera njira zolimbanira ndi mizimu yoipa.

VESI YOTSOGOLERA

Pamenepo ndidzatsika ndi kulankhula nawe komweko; ndipo ndidzatengako mzimu uti pa iwe, ndi kuika pa iwowa; adzakuthandiza kusenza katundu wa anthu awa, kuti usasenze wekha. (Numeri 11:17)

MAU OYAMBA

Mu chaputala ichi tiona njira imodzi ya mphamvu imene Satana amayigwiritsa ntchito. kuzindikira mfundo zimenezi kukunthandizani kuti mukhale ndi mayanku a zinthu zina zoipa zimene zakhala zikuchitika kwa anthu apabanja panu, anzanu, ngakhale kumvetsa nyengo zanu zomwe. Njira imene Satana amagwiritsa ntchito ndi kupatsirana mizimu.

ZITSANZO ZOCHITIKA MMOYO

choyambilira tiyenera kuona zitsanzo izi:

CHITSANZO CHOYAMBA:

Taganizirani za mwana wanu amene anakuzidwa ndi chikhalidwe chabwino. Iye amalemekeza malamuro amene munamupatsa ndipo mumapitira limodzi kutchalitchi ngati Banja. Koma mwadzi, mwana uja wangoyamba kuchita kusaweruzika, sakumveranso chilichonse chimene anauzidwa. Mwachitsanzo, iye wayamba kubwera kunyumba mochedwa. Ndizovuta kuti mumvetse kusintha kumeneku chifukwa ana ena amene muli nao sanayambepo achita zimenezi. Funso limene mukhoza kukhala nalo ndi lakuti: ndi chiani chimene chapangitsa kusintha kumeneku?

CHITSANZO CHACHIWIRI:

Otsatira kwa m’busa wina anali mdalitso waukulu kwambiri kumpingo. koma mwadzi anayamba kuonetsera kusakhutitsidwa, kutsutsana ndi zinthu, ndikusamvera ulamuliro wa m’busa wamkulu. Iye anapeza anthu amutsana amene amaonetsera chikhalidwe chofanana ndi

iye. Chifukwa cha ichi, m'busayu anadzala kusagwirizana pa mpingo. Ndipo izi zinabalaritsa nkkhosa.

KODI VUTO NDI CHIANI?

mutatati muunguze chitsanzo cha mwana chimene chaperekedwachi, kusingha kunabwera mwanayu atayamba kuyenda ndi munthu wina amene iye amamusilira. Mwina mkutheka kuti mwana wanu amakuuzani mmene makolo anzake amachitira ndi ana anzakewo. Chifukwa cha ichi, mwana wanu anayamba kusilira ndi kutengera khalidwe la mzakeyo.

Chimodzimidzi ndi chitsanzo cha m'busa chija, mukhoza kuona kuti iye amakonedwa ndi nkhosa zake. Chifukwa cha ichi, iye amamveredwa ndipo anatengerapo mwayi ndikuyamba kudzala mbeu ya kusagwirizana. Ndipo mzimu owukira ndi osaweruzika unafalikira mu mpingo onse.

KUPATSIRANA MIZIMU

Zitsanzo ziwiri zonsezi zaperekedwazi zinabwera chifukwa cha njira imodzi imene Satana amagwiritsa ntchito. Njira imene imatchedwa “kupatsirana mizimu.” Izi zimatanthauzauza kuti mzimu umachoka mwa munthu mmodzi kupita kwa munthu wina. Mau akuti “mzimu” malingana ndi phunziro ili amayimira “khalidwe” “kachitidwe kazinthu” Mau amenewa samatanthauza kupatsirana chiwanda.

China chilichonse chimene munthu amachita chimaonsetsera mzimu wina wake. mwachitsanzo, munthu akhoza kuonetsera mtima ofatsa, odzikuza kapena mtima owukira muzochita zake. Mzimu wa munthu umatha kukhudzidwa ndi mzimu wabwino kapena oipa ndipo munthu akhoza kupatsira anthu ene mzimu wake kapena kupatsira gulu la anthu limene.

Tisanaone zitsanzo za Baibulo zokhudzana ndi kupatsirana mizimu, ndikofunika kuti mumvetse mzimu wanu kaye. Ndikoyeneranso kumvetsa chifukwa chimene Satana amalimbana ndi mzimu wanu kwambiri. Muyenera kudziwa kuti Mulungu ndi amene analenga mzimu wanu.

Atero Mulungu Yehova, Iye amene analenga thambo, nalifutukula, nayala ponse dziko lapansi, ndi cimene cituruka m'menemo, Iye amene amapatsa anthu a m'menemo mpweya, ndi mzimu kwa iwo amene ayenda m'menemo; (Yesaya 42:5)

Ndi mzimu umene umapereka moyo.

Pakuti monga thupi lopanda mzimu liri lakufa, koteronso cikhulupiriro copanda nchito ciri cakufa. (Yakobo 2:26)

Pamene munthu amwalira, mzimu umabwelera kwa Mulungu:

Yehova, Mulungu wa mizimu ya anthu onse, aike munthu pa khamulo. (Numenti 27:16)

Komanso, tinali nao atate a thupi lathu akutilanga, ndipo tinawalemekeza; kodi sitidzagonjera Atate wa mizimu koposa nanga, ndi kukhala ndi moyo? (Ahebri 12:9)

Mulungu amayang'anira kapena kuweruza mzimu wanu:

Njira zonse za munthu ziyera pamaso pace; Koma Yehova ayesa mizimu. (Miyambi 16:2)

Cholinga cha Mulungu ndi chakuti aikize mzimu wake mwa inu amene ali Mzimu Woyera. Izi zimathandiza kuti mukhale paubale ndi Mulungu ndipo ichi ndi chifukwa chimene Satana amalimbana ndi Mzimu wanu.

Ndipo ndidzaika mzimu wanga m'kati mwanu, ndi kukuyendetsani m'malemba anga; ndipo mudzasunga maweruzo anga ndi kuwacita. (Ezekieli 36:27)

Mulungu akafuna asunge mzimu wanu muchiyero kufikira kubweranso kwa Yesu Khristu:

Ndipo Mulungu wa mtendere yekha ayeretse inu konsekonse; ndipo mzimu wanu ndi moyo wanu ndi thupi lanu zisungidwe zamphumphu, zopanda cirema pa kudza kwace kwa: Ambuye wathu Yesu Kristu. (1 Atesalonika 5:23)

Satana amalimbana ndi mzimu wa munthu chifukwa umachitira umboni wa Mzimu Woyera ndikupereka chitsikimizo cha chipulumutso.

Ndipo Mulungu wa mtendere yekha ayeretse inu konsekonse; ndipo mzimu wanu ndi moyo wanu ndi thupi lanu zisungidwe zamphumphu, zopanda cirema pa kudza kwace kwa: Ambuye wathu Yesu Kristu. (1 Atesalonika 5:23)

Chifukwa china ndi chakuti Mulungu amagwiritsa ntchito mzimu wanu ngati nyali ya moyo wanu. kudziko lakuthupi, nyali imapereka kuwala ndikuti munthu anthe kuona. Izi ndi chimodzimodzi ndi ntchito ya mzimu wanu mu dziko lauzimu:

Mzimu wa munthu ndiwo nyali ya Yehova; Usanthula m'kati monse mwa mimba. (Miyambi 20:27)

Satana amalimbana ndi mzimu wa munthu chifukwa amadzikwa kuti mu Ufumu wa Mulungu, Mulungu amagwiritsa ntchito munthu amene ali ndi mzimu woyenera.

Mzimu wa munthu ndiwo nyali ya Yehova; Usanthula m'kati monse mwa mimba. (Miyambi 20:27)

Satana amalimbana ndi mzimu chifukwa Mulungu amakhala mwa munthu amene ali ndi mzimu oyenera. Ndipo iye amabweretsanso chitsitsimutso pa munthu kudzera mu mzimu wa munthuyo.

Pakuti atero Iye amene ali wamtari wotukulidwa, amene akhala mwacikhalire, amene dzina lace ndiye Woyera, Ndikhala m'malo atari ndi oyera, pamodzi ndi

yense amene ali wa mzimu wosweka ndi wodzicepetsa, kutsitsimutsa mzimu wa odzicepetsa, ndi kutsitsimutsa mtima wa osweka. (Yesaya 57:15)

Pamene Satana abweretsa chisokonezo mu chiyanjano cha abale, cholinga chake ndi kulepheretsa chitsitsimutso mu mpingo. Satana amagwiritsa ntchito nkhondo yolimbana ndi mzimu wanu komanso amalimbana ndi lilirime lanu. Monga mmene taonera kale mu phunziro lamba, Satana amagwiritsa ntchito lilime ndi cholinga chofuna kubweretsa chim'bowo kapena chimphanga chimene oipayo akhoza kulowerapo.

Kuciza lilime ndiko mtengo wa moyo; Koma likakhota liswa moyo. (Miyambi 15:4)

Pamene Satana wakupangitsani inu kuti muchimwe chifukwa cha lilime lanu, iye amakhala kuti waika bowo limene zinthu zina zitha kulowa mumzimu wanu.

KODI KUPATSIRANA MZIMU KUMAGWIRIZANA NDI BAIBULO?

Kodi ndi zotheka kulandira mzimu wa munthu wina? Paulo anakambapo zakupatsirana mzimu

Pakutitu ngati iye wakudza alalikira Yesu wina, amene ife sitinalalikira, kapena ngati mulandira mzimu wa mtundu wina, umene simunalandira, kapena uthenga wabwino wa mtundu wina umene simunalandira, mulolana nave bwino lomwe. (2 Akorinto 11:4)

Pali zitsanzo zopezeka mu Baibulo zochotira umboni kupatsirana mzimu. Chitsanzo cha izi chikupezeka pa Numeri 11:16-17.

Ndipo Yehova anati kwa Mose, Undisonkhanitsire amuna makumi asanu ndi awiri mwa akuru a Israyeli, amene uwadziwa kuti ndiwo akuru a anthu, ndi akapitao ao; nubwere nao ku cihema cokomanako, kuti aimeko pamodzi ndi iwe. Pamenepo ndidzatsika ndi kulankhula nawe komweko; ndipo ndidzatengako mzimu uti pa iwe, ndi kuika pa iwowa; adzakuthandiza kusenza katundu wa anthu awa, kuti usasenze wekha. (Numeri 11:16-17)

NJIRA YA SATANA: KUPATSIRANA MZIMU OIPA.

Satana ndi munthu ongotengera zinthu, palibe chimene iye analenga. Iye amagwiritsa ntchito mfundo kapena chifaniziro chimene Mulungu anakhazikitsa chopatsirana mzimu wabwino pakati apa nthu. Chitsanzo chabwino ndi cha azondi amene Mose anawatuma kuti akazonde dziko la malonjezano. Werengani nkhani imeneyi pa Numeri 13:17;14 :39.

Khumi mwa azondi mwa otumidwa aja anabwera ndi zotsatira zosapatsa chiyembekezo. Iwo anapereka chithunzithunzi cha mdani wao amene anali wamphamvu kuposa iwo. Komanso apereka mantha chifukwa cha mafotokozeredwe awa a za chikupa chozungulira mizinda ya dziko lamalonjezano.

Koma anthu adakwera nayewo anati, Sitikhoza kuwakwerera anthuwo; popeza atiposa mphamvu, Ndipo anaipsira ana a Israyeli mbiri ya dziko adalizonda, nati, Dzikoli tapitamo kulizonda, ndilo dziko lakutheramo anthu okhalamo; ndi anthu onse tidaona pakati pace ndiwo anthu atali misinkhu. Tinaonakonso Anefili, ana a Anaki, obadwa ndi Anefili; ndipo tinaoneka m'maso mwathu ngati zinsidzi; momwemonso tinaoneka m'maso mwao. (Numeri 13:31-33)

koma awiri mwa azondi aja nali ndi mzimu osiyana ndi anzawo.

Ndipo Yoswa mwana wa Nuni, ndi Kalebi mwana wa Yefune, ndiwo a iwo aja adazonda dzikolo, anang'amba zobvala zao; nanena ndi khamu lonse la ana a Israyeli, nati, Dzikoli tapitamo kulizonda, ndilo dziko lokometsetsa ndithu. Yehova akakondwera nafe, adzatilowetsa m'dzikomo, ndi kutipatsa ilo; ndilo dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi. (Numeri 14:6-8)

Mukhoza kuona kuti apa panali mizimu iwiri yofuna kulamulira imene inali mwa azondi aja. Mizimu oyamba unali mzimu wakusakhulupirira ndipo mzimu wachiwiri unali wachikhulupiriro:

Koma Kalebi anatonholetsa anthu pamaso pa Mose, nati, Tikwere ndithu ndi kulilandira lathu lathu; popeza tikhozadi kucita kumene. (Numeri 13:30)

Taonani mmene mzimu opanda chikhulupiriro pakati pa azondi unasokonezera anthu.

Pamenepo khamu lonse linakweza mau ao, napfuula; ndipo anthuwo analira usikuwo. Ndipo ana onse a Israyeli anadandaulira Mose ndi Aroni; ndi khamu lonse linanena nao, Mwenzi tikadafa m'dziko la Aigupto; kapena mwenzi tikadafa m'cipululu muno! Ndipo Yehova atitengeranii kudza nafe kudziko kuno, kuti tigwe nalo lupanga? Akazi athu ndi makanda athu adzakhala cakudya cao; kodi sikuli bwino tibwerere ku Aigupto? Ndipo anati wina ndi mnzace, Tiike mtsogoleri, tibwerere ku Aigupto. (Numeri 14:1-4)

Pakati pa anthu paja panadzuka mizimu yakung'idza, kupanda chiyembekezo komanso kuukira. Koma mizimu yonseyi gwero lake linali azondi aja. Israeli sanakanike kulowa mudziko lamalonjezano chifukwa chakuti anali ndi ankhondo ochepa mphamvu ayi, koma iwo anakanika chifukwa cha mzimu yolakwika.

Ndichifukwa chiani anthu anakhudzidwa ndi mzimu oipa osati wabwino. Chifukwa chachikhalidwe chauchimo, anthu amakhulupilira mwachangu zonedwa zoipa. Ndipo chizolowezi chotsata chigulu ndi chimene nthawi zambiri munthu amachitenga ngati chifuniro cha Mulungu. Zinakhakhala kuti Israeli anavomereza zonena za Kalebu ndi anzake, uku kunakhakhala kuika moyo wao pachiopezo. Izi zili chomwechi, chifukwa mwachikhalidwe chathu chaumunthu, timafuna zinthu zophweka.

Khondo zambiri zauzimu zimene okhulupirira amakumana nazo zimabwera chifukwa chakupatsirana mizimu. Komanso kupatsirana mizimu kumabweretsa kusintha kwa khalidwe

kuchoka pa khalidwe labwino kipita pa khalidwe loipa. Kupatsirana mizimu kukhoza kufotokozera chifukwa chimene ana amene aleleredwa bwino amasinthwa mosadziwika bwino. Komanso ndi chifukwa chimene chimabweretsa mpungwepungwe mumpingo. Pamene mwachita ubale ndi munthu amene ali ndi mzimu wamphamvu kwambiri kuposa wanu, mumatha kutengera mzimu wamunthuyo ndipo mumasinthika chifukwa cha mzimu mwalandirawo.

NJIRA ZOLIMBANIRA NDI KUPATSIRANA MZIMU OIPA.

Mulungu wapereka njira zolimbana ndikupatsirana mzimu oipa:

MUYENERA KUYANG'ANIRA MZIMU WANU:

Muyenera kuyang'anira mzimu wanu poonetsetsa kuti simukukuza mzimu olakwika umene mukhoza kupatsira anthu ena:

**Wosalamulira mtima wace Akunga mudzi wopasuka wopanda linga,
(Miyambi 25:28)**

Pakuti ndidana nako kuleka kumene, ati Yehova Mulungu wa Israyeli, ndi iye wakukuta cobvala cace ndi ciwawa, ati Yehova wa makamamu; cifukwa cace sungani mzimu wanu kuti musacite mosakhulupirika. (Malaki 2:16)

TCHINJIRIZANI LILIME LANU:

**Cinjiriza mtima wako koposa zonse uzisunga; Pakuti magwero a moyo aturukamo
(Miyambi 4:23).**

Muyenera kuyang'anira zinthu zimene mumakonda. Simukuyenera kupereka chikondi kapena ulemu wanu kwa wina aliyense. Mukhoza kuika polowera pamene anthu amene mumawakonda akhoza kulowetsa mzimu wao pa inu.

SANKHANI MOSAMARITSA ABWENZI ANU:

Buku la Miyambo limachenjeza kuchit ubale ndi anthu amene ali ndi mzimu oipa. Mwachitsanzo, pa Miyambo 1:10-19 ndi 2:11-22 tikuchenjezedwa kuti:

**Usayanjane ndi munthu wokwiya msanga; Ngakhale kupita ndi mwamuna waukali;
Kuti ungaphunzire mayendedwe ace, Ndi kutengera moyo wako msampha,
(Miyambi 22:24-25)**

**Usalowe m'mayendedwe ocimwa, Usayende m'njira ya oipa. Pewapo, osapitamo;
Patukapo, nupitirire. Miyambi 4:14-15**

Pita pamaso pa munthu wopusa, Sudzazindikira milomo yakudziwa. Miyambi 14:7

**Ngamene acedwa pali vinyo, Napita kukafunafuna vinyo wosanganizidwa.
(Miyambi 23:30)**

**Woyenda ndi mbala ada moyo wace wace; Amva kulumbira, koma osaulula kanthu.
(Miyambi 29:24)**

Ngati mumayenda ndi anthu a nzeru, mzimu wao umalowa mwa inu:

**Ukayenda ndi anzeru udzakhala wanzeru: Koma mnzao wa opusa
adzaphwetekedwa. (Miyambi 13:20)**

Muyenera kusankha mosamaritsa abwenzi anu. Ndipo ngati muli makolo, muyenera kuunikira abwenzi amene ana anu ameyenda nao.

TCHINJIRIZANI ZIMENE THUPI LANU LIMAFUNA

Kumbukirani zimene tinapuzira zokhudza thupi, tinaphuzira kuti muyenera kutchinjiriza zimene mumamva, kaya ndi mabodzo kapena miseche, kuipitsa mbiri ya anthu ena. Izi zikhoza kupangitsa kuti mukuze mzimu wachilendo. Muyeneranso kutchinjiriza maso anu kuzimene mumaonera mwachitsanzo zinthuzi za kanema olaura, kapena kuwerenga ndi kuonera zinthu zimene mukhoza kupara mzimu wa chigoloro, dama ndi chiwawa.

SAMALITSANI NDI ANTHU OKUSANJIKANI MANJA:

Kusanjika manja ndi maziko amodzi a chikhristu amene Paulo anawafotokoza mu Buku la Ahebri 6:1-3. Kusanjika manja kuli ndi cholinga chapadera chimene chafotokozeredwa kale mu phunziro lina la Haverstime International Institute lotchedwa “Maziko A Chikhulupiuro”

Chimene muyenera kuzindikira ndi chakuti mzimu timatha kupatsirana ngati mmene Mose anaonetsera ndi akulu makumi asanu aja. Mzimu akhoza kuperekedwa posanjika manja. Ngati mzimu wabwino umaperekedwa kudzera kusanjika manja, ndi zothekanso kuti anthu akhoza kupatsana mzimu oipa kudzera munjira yomweyi. Chifukwa cha ichi, muyenera kusamaritsa ndi anthu amene angakusanjikeneni manja kuti mulandire kudzodza kwauzimu.

KUYENDERA PARETE

1. lembani vesi yotsogolera kuchokera muzolemba zankhondo.

2. kodi “kupatsirana mizimu ndi chiani”?

3. Perekani chitsanzo chopeza mu Baibulo chopatsirana mzimu wabwino

4. Perekani chitsanzo chimodzi chopezeka mu Baibulo chopatsirana mzimu oipa?

5. Tchulani njira zisanu ndi imodzi yolimbani ndi kupatsirana mizimu yoipa.

(mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa Buku ili)

MACHITACHITA ALUSO

1. Werengani zokhudza kupatsirana mzimu wabwino. Mneneri Elisa anatola chofunda cha mneneri Eliya. Chofunda chimenechi chimaimira mzimu wa Mulungu umene unali mwa Eliya. Elisa anapempha magawo awiri a mzimu wa mneneri wa Eliya. Werengani nkhani imeneyi pa 2 Mafumu chaputala 2
2. Werengani nkhani ya Ananiya ndi Safira. Ichi ndi chitsanzo chimene bambo anapatsira mzimu wake wachinyengo mkazi wake.
3. Werengani ma vesi ali munsimu amene akuonetsera kuti mzimu wanu ukhoza kukhudzidwa ndi zinthu zina zabwino komanso zoipa. Chifukwa cha izi, mzimu wanu ukhoza kukhala mu zithu izi:

Nsanje: Numeri5:14

Kuumitsa mtima: Deteronome 2;30

Kuwawa mtima: Eksodo 6:9

Wabwino: Nehemiya 9:20

Opanda chinyengo: Masalimo 32:2

Oyenera: Salimo 51:10

Osweka: Salimo 51:17

Kuthodwa: Salimo 77:3; 142:3; 143:4

Olimbika ndi osanthula: Salimo 77:6

Ogwiritsa: Salimo 78:8

Olephera mwa iye yekha: Salimo 143:7

Okhulupirika: Miyambo 11:13; II Akorinto 4:13

Ofulumira: Miyambo 14:29; Mlaliki 7:9

Odzikuza: Miyambo 16:18

Odzichepetsa: Miyambo 16:19

Kuvulara: Miyambo 18:14

Kugwira njakata: Mlaliki 1:14

Odekha: Mlaliki 7:8

Wodzikuza mtima: Mlaliki7:8

ofunafuna: Yesaya 26:9

Oweruza: Yesaya 28:6

Okhala mu zolakwika: Yesaya 29:24

Odzichepetsa ndi wachisoni: Yesaya 57:15

Osauka ndi achisoni: Yesaya 66:2

Achete: Zakariya 6:8

Waluntha: Danieli 5:12; 6:3

Olira: Danieli 7:15

Wanzeru: Ekodo 28:3

Wamphamvu: Luka 2:40

Olakwitsa: Luka 9:55

Wopembedza: Yohane 4:23-24; Afilipi 3:3
 Osautsika: Genesis 41:8; Danieli 2:3; Yohane 13:21; II Atesalonika 2:2
 Kutsikimikizika: Machitidwe 6:10
 Kusunthika: Ezara 1:1; Hagayi 1:14; Machitidwe 7:16
 Kuphinjidwa: Machitidwe 18:5
 Achangu: Machitidwe 18:25; Aroma 12:11
 Omangidwa: Machitidwe 20:22
 Otumukira: Aroma 1:9
 Odulidwa Aroma 2:29
 Watsopano: Ezekieli 11:19; 18:31; 36:26; Romans 7:6
 Musinga: Aroma 8:15
 Kuchitira umboni ndi Mzimu wa Mulungu: Romans 8:16
 Kugona: Aroma 11:8
 Ofatsa: Agalatiya 6:1
 Wofatsa ndi wachete: I Petro 3:4
 Wapemphero: I Akorinto 14:14;
 Amodzi ndi Mulungu: I Akorinto 6:17
 Kulemekeza Mulungu I Akorinto 6:20
 Maimbidwe: I Akorinto 14:15
 Kutsitsimutsa: I Akorinto 16:18; II Akorinto 7:13
 Osakhazikika: II Akorinto 2:13
 Onyasa: II Akorinto 7:1
 Oyanjanitsidwa ndiokhulupirira ena: II Akorinto 12:18; Philippians 1:27
 Kusingidwa: I Atesalonika 5:23
 Chitsanzo kwa okhulupirira: I Timothy 4:12
 Wamantha: II Timoteyo 1:7
 Azilakolako: Yakobo 4:5
 Ofuna/ okonzeka: Ekosodo 35:21; Mateyu 26:41
 Osauka: Mateyu 5:3
 Watcheru: Marko 2:8
 Okonzeka: Marko 14:38
 Wachisoni: I Samueli 1:15
 Osakondwa: I Mafumu 21:5
 Wachimweme: Luka 1:47
 Kuusa moyo: Marko 8:12

4. Kodi mumaona ngati munapatsidwa mzimu oipa? Kodi ndi ndani amene mukuona ngati anakhudza mzimu wanu? Kodi zotsatira za kupatsiridwa mzimu osakhala bwinou chinali chiyani? Ngati munakhudzidwa ndi mizimu yoipa, mukhoza kudzitchinjiriza potsata njira zimene zatchulidwa mu chaputala ichi.
 - Kuyang'anira mzimu wanu.

- Kutchinjiriza lilime lanu.
 - Kuyang'anira zinthu zimene mumakonda.
 - Kusankha mosamaritsa anthu amene mumacheza nao.
 - Kuyang'anira zofuna zathupi lanu.
 - Kusamalitsa ndi amaene angakusanjikeneni manja.
5. Pali mphatso yapadera ya Mzimu Woyera imene ndi mphatso yachidziwitso. Mpatsoyi imathandiza okhulupirira kuti athe kuzindikira mzimu oipa kapena wabwino. Mukhoza kuphunzira zambiri za mphatso za Mzimu Woyera mu phunziro lina la Harvestime Internation Institute lotchedwa “Utumiki wa Mzimu woyera”

CHAPUTALA 20

CHOIPA MUUZIMU MUMAGUWA AM'MWAMBA

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsegolera osaonera.
- Kufotokozerana tanthauzo la “kuipa muuzimu m’magome”.
- Kufotokozerana njira zimene Satana amagwiritsa mu gawo limeneli.
- Kuzindikira njira zothana ndi kuipa muuzimu m’magome.

YESI YOTSOGOLERA KUCHOKERA MUZOLEMBA ZA NKHONDO:

Ndipo kulibe kudabwa; pakuti Satana yemwe adzionetsa ngati mngelo wa kuunika. Cifukwa cace sikuli kanthu kwakukuru ngatinso atumiki ace adzionetsa monga atumiki a cilungamo; amene cimariziro cao cidzakhala monga nchito zao. 2 (Akorinto 11:14-15)

Munaphunzira kuti nkhondo yauzimu si yamwazi ndi thupi. Komanso mwaona m’mene mphamvu zakumidima zimagwilira ntchito. Koma chaputala ichi chikhazikika pa gawo lina la asirikali a Satana limene ndi la auzimu a choipa m’nzamwamba.

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

MAGOME

Mwachikhalidwe chatu ngati anthu, nthawi zambiri chithuzithuzi chimene timakhala nacho cha Mulungu ndi chakuti amakhala mlengalenga kapena m’mwamba. Kuchokera pachiyambi, anthu akhala akusankha malo okwera kapena kuti am’mwamba ngati malo opembedzera Mulungu weniweni kapena milungu yopangidwa ndi munthu. Mu Chipangano chakale, malo am’mwamba anali malo amene amakhudzana ndi kupereka nsembe, kupembedza mafano komanso anali malo azikondwewero zoipa. Mulungu analamura ana a Israeli kuti pamene alowa mu dziko lamalonjezano, athamangitse onse akukhalamo mu dzikolo ndi kuononga misanja yawo.

mupitikitse onse okhala m'dzikopamaso panu, ndi kuononga mafano ao onse a miyala, ndi kuononga mafano ao onse oyenga, ndi kupasula misanje yao yonse; (Nomeri 33:52)

Buku la oweruza limafotokoza kulephera kwa Israeli kuti apirikitse anthu onse okhala mudziko lamalonjezano. Chifukwa chaichi, iwo anayamba kupembedza milungu yachilendo mumisanja.

Itatha nyengo imeneyi, ena mwamafumu angwiro anaongonga misanja imeneyi. Koma ena anamanganso misanjayi nayamamba kupembedza milungu ya chilendo.

Mfumu Mananse inali mfumu imodzi imene inamanga nsanja yopembedzera mafano. Koma atalandira chilango, analapa ndipo anabwezeletsedwa ngati mfumu. Ndipo iye anabwelera kuchipembedzo choyenera. Anthu nthawi imeneyi anali kuperekabe nsembe mumisanja, koma Mulungu anakhudza mitima yawo (2 Mbiri 33).

Mulungu ataitana Gideiyozi ngati wankhondo wamphamvu, Iye anamulamula kuti agwetse guwa lansembe ndi kulikha chifaniziro. Iye anauzidwanso kuti amange guwa lansembe la Mulungu. Ndipo Mulungu analamura Gideoni kuti apereke nsembe yopsereza kwa Mulungu. koma kuti izi zichitike, Gideoni amayenera kugwetsa guwa lamafano kaye. Chifukwa chaichi, chiomboro chinadza pa ana a Israeli. Lero lino Mulungu akuitanabe anthu kuti awononge maguwa ansembe apamwamba ndi ankhondo ake amphamvu.

NJIRA IMENE SATANA AMAGWIRITSA NTCHITO:

KUIPA MUUZIMU MUMAGUWA APAMWAMBA.

Pamene Paulo amakamba za kuipa muuzimu m'malo am'mwamba, Iye amafotokozera za mizimu yoipa imene yafalikira mapembedzedwe adziko lapansi. Mizimu imeneyi yafalikira muzipempedzo za anthu oyera mtima. Satana wasonkanitsa ankondo ake kuti achite zinthu zokhala ngati zofanana ndi mpingo wa Mulungu. Ndipo anafika poyambitsa chipembedzo chotchedwa mpingo wa Satana. Iye wakhazikitsa mapembedzedwe m'malo amwamba auzimu.

Komanso Satana walimbikitsa zipembedzo zonyenga zimene zimabisa zochita zawo zenizeni. Zipembedzo zonyengazi zilinso m'gawo limodzo la nyanga kapena ufiti. Awa ndi anthu amene amabisa ntchito zao zoipa ndi mwinjiro wachipembedzo. Koma choopsya kwambiri ndi chakuti satana wakhazikitsa mizu yake ndi mumpingo wa Mulungu omwe kudzera mwa anthu oipa amane alowa mwakachetechete. (Yuda 4)

Kudzera kuipa muuzimu m'maguwa amwamba, cholinga cha Satana ndi choti anthu onse amvera iye. Iye amagwiritsa ntchito zipembedzo zonyenga, mpingo wake umene ndi mpingo wa Satana komanso kulowelera mu mpingo wa Mulungu mwakachetechete kuti akwaniritse zolinga zake. Izi ndi zimene Baibulo limaphunzitsa za dongosolo la bungwe lachipembedzo la Satana:

SATANA ALI NDI UTATU WAKE:

Munaphunzira muphunziro lina za Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Naye Satana ali ndi utatu wake umene ndi Iye mwin Satana, Chilombo ndi mneneri onyenga. Muphunzira za Chilombo ndi mneneri onyenga mu chaputala chapatsogolo. Mu Buku la Chivumbulutso, Yohane akufotokoza za chionongeko cha anthu atatu amenewa:

Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyedwa m'nyanja ya mota ndi sulfure, kumeneko kulonso ciomboco ndi mneneri wonyengayo; ndipo adzazunzidwa usana ndi usiku ku nthawi za nthawi. Cibvumbulutso 20:10

SATANA ALI NDI MPINGO WAKE:

Mulungu anakhazikitsa mpingo wake umene ndi thupi la Khristu Yesu ndipo mutu wa thupi limeneli ndi Yesu Khristu.

Koma inundinu thupi la Kristu, ndi ziwalo, yense pa yekha. (1 Akorinto 12:27)

koma ndi kucita zooni mwa cikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira iye amene ali mutu ndiye Kristu; kucokera mwa Iye thupi lonse, lokowanidwa ndi lolumikizidwa pamodzi, pothandizanapo mfundo yonse, monga mwa kucititsa kwa ciwalo conse pa muyeso wace, licita makulidwe a thupi, kufikira cimango cace mwa cikondi. (Aefeso 4:15-16)

Satana naye ali ndi mpingo wake umene umatchedwa Sunagogi wa Satana:

Ndidziwa cisautso cako, ndi umphawi wako (komatu uli wacuma), ndi mwano wa iwo akunena za iwo okha kuti ali Ayuda, osakhala Ayuda, komatu sunagoge wa Satana. (Cibvumbulutso 2:9)

Mau oti Sunagogi wa Satana amayimira malo ena alionse amene Uthenga Wabwino Sumalalikidwa.

SATANA NAYE ALI NDI CHIPHUNZITSO CHAKE:

Baibulo ndi lodzala ndi chiphunzitso choonadi cha Mulungu chimene chavumbulutsidwa ndi Mzimu Woyera:

Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: (2 Timoteo 3:16)

Chiphunzitso cha Satana chimatchedwa “chiphunzitsa cha ziwanda”

Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m'masiku otsiriza ena adzataya cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunziro a ziwanda, (1 Timoteo 4:1)

Gawo limodzi la mitundu ya ziwanda limatchedwa “mizimu yonyenga.” Cholinga cha mizimu imeneyi ndi kukopa anthu kuziphunzitso zonyengo. Chiphunzitso chaziwanda ndi chiphunzitso china chilichonse chimene chimaphunzitsidwa ngati choonadi koma choonadi chake ndi chakuti izi zimakhala zosemphana ndi mau a Mulungu.

SATANA ALI NDI NJIRA ZOPEREKERA NSEMBE:

amafotikoza kuti tiyenera kupereka matupi athu ngati nsembe zamoyo. Izi zikutanthauza kuti tiyenera kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu. Koma naye Satana naye amafunanso nsembe: (Aroma 12:1)

Koma nditi kuti zimene amitundu apereka nsembe azipereka kwa ziwanda; ndipo sindifuna kuti inu muyanjane ndi ziwanda. (1 Akorinto 10:20)

Satana naye amafuna kuti tidzipereke kwa Iye ndi thupi lathu lonse, mzimu wathu ndi mzeru zathu zonse. Izi ndi nsembe zimene anthu amepereka pamene adzipereka kutumikira Satana. Nthawi zina nsembe za mwazi wa anthu ndi nyama zimaperkedwanso.

NAYE SATANA ALI NDI MGONERO WAKE:

Kuchita chiyanjano kudzera mumgonero ndi chinthu chimene chinakhazikitsidwa ndi Yesu Khristu ngati njira imodzi yokumbukira nsembe yochotsa machimo imene inaperkedwa kwa anthu onse pamtanda. (1 Akorinto 11:23-34). Koma naye Satana ali ndi mgonero wake wachinyengo.

Koma nditi kuti zimene amitundu apereka nsembe azipereka kwa ziwanda; ndipo sindifuna kuti inu muyanjane ndi ziwanda. (1 Akorinto 10:20)

ATUMIKI A SATANA AMALALIKIRA UTHENGA WAKE:

“Uthenga wa Satana ndi osemphana ndi Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu Khristu:

umene suli wina; koma pali ena akubvuta inu, nafuna kuipsa Uthenga Wabwino wa Kristu. Koma ngakhale ife, kapena mngelo wocokera Kumwamba, ngati akakulalikireni uthenga wabwino wosati umene tidakulalikirani ife, akhale wotembereredwa. (Agalatiya 1:7-8)

SATANA NAYE ALI NDI MPANDO WACHIFUMU:

Mulungu ali ndi mpando wachifumu kumwamba, koma nayenso Satana ali nao mpando wake wachifumu ngakhale kuti kumene kuli mpandou sikudziwika:

Ndipo cirombo ndinacionaco cinafanana ndi nyalugwe, ndi mapazi ace ngati mapazi a fisi, ndi pakamwa pace ngati pakamwa pa mkango; ndipo cinjoka cinampatsa iye mphamvu yace, ndi mpando wachifumu wace, ndi ulamuliro waukuru. (Cibvumbulutso 13:2)

SATANA ALI NDI OMPEMBEDZA AKE:

Opembedza a Mulungu weniweni ndi ambiri koma naye Satana ali ndi ompembedza ake:

Ndipo cirombo ndinacionaco cinafanana ndi nyalugwe, ndi mapazi ace ngati mapazi a fisi, ndi pakamwa pace ngati pakamwa pa mkango; ndipo cinjoka cinampatsa iye

**mphamvu yace, ndi mpando wacifumu wace, ndi ulamuliro waukuru.
(Cibvumbulutso 13:2)**

Koma ena mwa opembedza Satana amanamizira kukhala ngati otsatira a Yesu Khristu:

ndipo munda ndiwo dziko lapansi; ndi mbeu yabwino ndiyo ana a Ufumuwo; ndi namsongole ndiye ana a woipayo; ndipo mdani amene anamfesa uwu ndiye mdierekezi: ndi kututa ndico cimariziro ca nthawi ya pansi pano; ndi otutawo ndiwo angelo (Mateyu 13:38-39)

Satana amaphatikiza mbeu yoipa ndi yabwino (okhulupirira).

SATANA ALI NDI ANENERI ONYENGA:

Mulungu anakhazikitsa aneneri ake mumpingo. Awa ndi anthu amene amalandira uthenga ochokera kwa Mulungu kupita kumpingo wake. (1 Akorinto 12: 28) Satana ali ndi aneneri ake amene amapereka mau a uneneri onyenga:

Ndipo aneneri onama ambiri adzauka, nadzasokeretsaanthuambiri. (Mateyu 24:11)

SATANA ALI NDI APHUNZITSI AKE:

Mulungu anadzodza anthu ena mumpingo ngati aphunzitsi oti akaphunzitse ndi kufotokozera mau ake kwa anthu ena. (1 Akorinto 12:28). Koma aphunzitsi ena ndi a Satana amene cholinga chao ndikufalitsa chiphunzitso chonyenga ndi choipa:

Koma padakhalanso pakati pa anthuwo aneneri onama, monganso padzakhala aphunzitsi onama pakati pa inu, amene adzalowa nayo m'tseri mipatuko yotayikitsa, nadzakana Ambuye amene adawagula, nadzadzitengera iwo okha citayiko cakudza msanga. Ndipo ambiri adzatsata zonyansa zao; cifukwa ca iwo njira ya coonadi idzanenedwa zamwano. Ndipo m'cisiro adzakuyesani malonda ndi mau onyenga; amene ciweruzo cao sicinacedwa ndi kale lomwe, ndipo citayiko cao siciodzera. (2 Petro 2:1-3)

Aphunzitsi a Satana amaphunzitsa ziphunzitso zonyenga ndipo ziphunzitso zimene amaphunzitsa zimabweretsa kugawikana pa mpingo. Chimene amalakhula ndi bodzo ndipo iwo ndi akatswiri odziwa kusakanika bodza ndi choonadi munjira imene imapanga bodzo kukhala choonadi. Ziphunzitso zonyenga ndi zimene zimabweretsa kuphukira kwa zipembedzo zonyenga. Chipembedzo chonyenga ndi njira yakapembedzedwe imene imakhala yosemphana ndi mau a Mulungu m' ma gawo ena.

Mayina, ziphunzitso ndi kayendetsedwa ka zipembedzo zonyenga kamakhala kosiyanasiyana. Ndizovuta kutchula mayina onse azipembedzo zonyenga chifukwa alipo ambiri. Koma chimene muyenera kukumbukira ndi chakuti, chipembedzo china chilichonse chimene ndi chosemphana ndi mau a Mulungu ndi chipembedzo chonyenga (mu gawo la zoonjezera pophunzira muphunzira zambiri zakazindikiridwe ka zipembedzo zonyenga.

SATANA NAYE ALI NDI ATUMWI AKE:

Mtumwi ndi munthu amene amafalitsa Uthenga Wabwino ndi kudzala mipingo (1 Akorinto 12: 28). Koma naye Satana ali ndi atumwi ake pa dziko lonse lapansi. Iwo amasocheretsa anthu ambiri ponamizira ngati atumwi a Mulungu:

Pakuti otere ali atumwi onyenga, ocita ocenjerera, odzionetsa ngati atumwi a Kristu, (2 Akorinto 11:13)

Atumwi a Satana amatsogolera zipembedzo zonyenga mu maudindo autsogoleri.

SATANA AMATENGERA YESU KHRITSU KUDZERA MWA A YESU ABODZA:

Kudzuka kwa a Yesu abodza zimaonetsera kuti Satana amatengera Yesu Khristu. Yesu anachenjeza za izi:

Ndipo Yesu anayankha nati kwa iwo, Yang'anirani, asasokeretse inu munthu. Pakuti ambiri adzafika m'dzina langa, nadzanena, Ine ndine Kristu, nadzasokeretsa anthu ambiri. (Mateyu 24:4-5)

SATANA ALI NDI NJIRA ZAKE ZOLANKHULIRA:

Baibulo ndi umboni wa mmene Mulungu analankhulira kwa munthu ndipo iye akupitiriza kulankhulabe kwa anthu lero lino. (pali phunziro lapadera la Harvestime Internationala ministries limene limakamba za kuzindikira kulankhula kwa Mulungu.) koma nayenso Satana amayankhula kwa munthu ndipo zotsatira za mau ake kwa munthu zinali tchimo. Izi zinachitika mmunda wa Edeni. (Genesis 3)

Okhulupirira amapempha zosowa zao kwa Mulungu kudzera mupemphero ndipo Mulungu amayankha maphero a anthu oyera mtima. (Yakobo5:16). Koma naonso otsatira Satana amapempha kwa iye ndi kulankhula ndi mizimu yoipa. Nthawi zina Satana amayankha mapemphero a anthu ake kudzera muzodabwitsa monga phokoso, zinthu kumangoyenda pazokha ndi zina zambiri.

Mulungu analankhula kwa munthu kudzera mmawo ake olembedwa. Koma nayenso Satana akulankhula kudzera muzinthu zolembedwa monga mabuku, zithunzi zakanema ndi nyimbo. Cholinga cha kulankhula kwa Mulungu kudzera mu mau ake olembedwa ndi kupereka chitsogozo kwa munthu pa zochitika za moyo. Koma Satana amaperekanso chitsogozo chabodza kudzera munjira izi:

Ufiti: izi zimakhudza zinthu ngati, nyanga, maula, kuombeza, zithumwa ndi njira zina zopezera chitsogozo koma zosemphana ndi Baibulo.

SATANA ALI NDI MPHAMVU ZODABWITSA:

Yesu Khristu analonjeza mphamvu ya zodabwitsa kwa ophunzira ake pamene adzalandira mzimu wake. Satananso amapereka mphamvu zodabwitsa ndi ulamulira kwa omutsatira ake

(Chibvumbulutso 13:2). Ziwanda zake zikhoza kupereka mphamvu yodabwitsa. Satana amathanso kuchita zizindikiro ndi zozizwitsa:

pakuti ali mizimu ya ziwanda zakucita zizindikilo; (Cibvumbulutso 16:14)

. Yesu anati:

Ambiri adzati kwa Ine tsiku lomwelo, Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kuturutsa mizimu yoipa, ndi kucita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri? Ndipo pamenepo ndidzafukulira iwo, Sindinakudziwani inu nthawi zonse; cokani kwa Ine, inu akucita kusayeruzika. (Mateyu 7:22-23)

NJIRA ZAUZIMU ZOLIMBANIRANA NDI KUIPA MUUZIMU MMALO AM'MWAMBA/ MAGOME AMWAMBA.

Izi ndi njira zothanira ndi kuipa muuzimu magome a m'mwamba.

SINDIKIRANI KUTI SATANA NDI ONGOTENGERA:

Malingana ndi phunziro limeneli, pamene mwafikapa muyenera kuzindikira kuti Satan ndi ongotengera. Chifukwa cha ichi, muyenera kudziwa kuti Satana amayesetsa kuchita zinthu mofana ndi zinthu za Mulungu. Choncho, muyenera kukhala osamalitsa ndi maonekedwe okhala ngati a Mulungu.

GWIRITSANI NTCHITO CHIDZIWITSO;

Pali mpatso yapadera ya mzimu Woyera imene imatchedwa mpatso yachidziwitso. Iyi ndi mphatso yotha kudziwa mzimu wa munthu wina ngati uli wabwino kapena oipa. Ngati muli ndi mphatso ya mzimu umeu, igwiritseni ntchito mpatsoyi kuti muthane ndi kuipa muuzimu m'magome a m'mwamba.

Ngati tilibe mpatso yachidziwitso, Mulungu wapereka njira ina imene tikhoza kugwiritsa ntchito kuzindikira mizimu yonyenga. II Petro ndi Buku la Yuda lafotokozera chikhalidwe cha anthu amene ali ndi mizimu yonyenga. Okhulupirira tonse tikulimbikitsidwa kuti tiyese mizimu (I Yohane 4:1) Kuyesa mzimu kapena mizimu sizitanthauza kuti mulibe chikhulupiriro. Koma ngati mizimu ili ya Mulungu, imapambana mayeso amene imapatsidwa.

WERENGANI MAU A MULUNGU:

Kuti mukathe kuzindikira ziphunzitsa zonyenga za aneneri, atumwi ndi aphunzitsi, muyenera kudziwa zimene Baibulo limaphunzitsa. Paulo anachenjeza Timoteyo motere:

Ucite cangu kudzionetsera kwa Mulungu wobvomerezeka, wanchito wopanda cifukwa ca kucita manyazi, wolunjika nao bwino mau a coonadi. (2 Timoteyo 2:15)

Posatengera kuti Paulo anali mtsogoleri wazauzimu wamkulu mumpingo oyamba, koma okhulupirira aku Bereya anasathura malemba kuti awone ngati zimene Paulo amakamba zinali zogwirizana ndi Baibulo.

Amenewa anali mfulu koposa a m'Tesalonika, popeza analandira mau ndi kufunitsa kwa mtima wonse, nasanthula m'malembo masiku onse, ngati zinthu zinali zotero. (Macitidwe 17:11)

kuti mupewe kunamizidwa ndi choipa chauzimu m'magome, ndikofunika kuti muunguze chilichonse chophunzitsidwa malinga ndi mau a Mulungu.

MUKANE CHINA CHIRICHONSE CHIMENE SICHIRI M'MALEMBA:

Satana anakhazikitsa choipa chauzimu m'magome am'mwamba kudzere mu mabvumbulutso a choonadi chatsopano. Anthu nthawi zina amatha kunena kuti alandira vumbulutso latsopano kudzera kumaloto, kuonekeredwa ndi angero, masomphenya ndi njira zina zolandilira mavumbulutso. Koma Paulo akuchenjeza:

umene suli wina; koma pali ena akubvuta inu, nafuna kuipsa Uthenga Wabwino wa Kristu. Koma ngakhale ife, kapena mngelo wocokera Kumwamba, ngati akakulalikireni uthenga wabwino wosati umene tidakulalikirani ife, akhale wotembereredwa. (Agalatiya 1:7-8)

Muyenera kukana chiphunzitso, vumbulutso kapena chionetsera chilichonse chimene ndi chosemphana ndi mau a Mulungu (Aroma 18:22) Simuyenera kuvomereza chiphunzitso chinachilichonse chimene chikhoza kukuchotsani pamaso pa Mulungu ndi pachoonadi cha mau ake (Deteronome 13:1-5)

Munthu wosocera pa njira ya nzeru Adzakhala m'msonkhano wa akufa. (Miyambi 21:16 16)

MUYENERA KUUNGUZA CHIPATSAO CHAUZIMU

Chifukwa chakuti satana ndi ongotengera zimene mphamvu ya Mulungu imapanga kudzera muzodabwitsa zake, Muyenera kuunikira kapena kusanthula zinthu zauzimu poyang'anira chipatso chauzimu:

Yesu Khristu anafananitsa munthu ndi chipatso cha mtengo. Iye anati tidzawadziwa atumiki ake enieni ndi onyenga ndi zipatso zawo:

Sungathe mtengo wabwino kupatsa zipatso zoipa, kapena mtengo wamphuci kupatsa zipatso zokoma. Inde comweco pa zipatso zao mudzawazindikira iwo. (Mateyu 7:18,20)

Satana amatha kutengera mpatso zauzimu za Mulungu, koma iye chimene sangakwanitse ndi kutengera chikhalidwe cha moyo wachiyero umene umaonetsera chipatso cha Mzimu Woyera. Zina mwazipatso za mzimu woyera ndi izi:

cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupirtro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. (Agalatiya 5:22-23)

Chifukwa cha ichi, muyenera kusanthula kapena kuunikira munthu malinga ndi zipatso osati chionetsera cha mphamvu.

PEWANI CHIRICHONSE CHOKHUDZANA NDI SATANA:

Mulungu anachenjeza kuti tipewe china chilichonse cha Satana:

mupitikitse onse okhala m'dzikopamaso panu, ndi kuononga mafano ao onse a miyala, ndi kuononga mafano ao onse oyenga, ndi kupasula misanje yao yonse; (Numenti 33:52)

werengani malangizo apadera amene Mulungu anapereka kwa Israeli pa Deteronome 18:9-14. Israeli samayenera kukhudzidwa ndi ntchito ina iliyonse ya Satana. Ife lero lino tiyenera kuononga china chilichonse chokhudzana ndi ufiti kapena ntchito za Satana. Zina mwa zinthu zimenezi ndi izi: zithumwa, mafano, mikanda ndi zina zambiri. Izi ndi zimene anthu ena anachita mu Chipangano chatsopano atakhulupirira Mulungu:

Ndipo ambiri a iwo akucita zamatsenga anasonkhanitsa mabuku ao, nawatentha pamaso pa onse; ndipo anawerenga mtengo wace, napeza ndalama zasiliva zikwi makumi asanu. (\$9,300). (Macitidwe 19:19)

Muyenera kuononga zolembedwa zina zilizonse zimene sizilemekeza Mulungu. Simukuyenera kukhala malo amene pali mphamvu ya oipa. Baibulo limaonetsera kuti Mulungu anadzionetsera yekha mmalo apaderadera monga ngati mukachisi wa Chipangano Chakale ndi mu chipinda chapamwamba pa tsiku la Pentekoste. Izi zikutanthauza kuti mphamvu za Satana zikhoza kuonekera malo ena alionse amene anaperekedwa kwa Satana. Malo amenewa akhoza kukhala malo amene kanema olaura amaonetsedwa, malo amene mowa ukumwedwa komanso pali khalidwe lachipolowe. Kapena mwachidure malo ena alionse amene mtchitidwe wauchimo ukuchitika. Chifukwa cha ichi, mukuyenera kupewa malo ngati amenewo chifukwa mphamvu ya Satana imakhala yamphamvu. Ndizovuta kuti mupemphera kwa Mulungu kuti akulanditseni kumayesero malo ngati amenewa pamene kwinaku mukupitiriza kukhalabe malo ngati amenewo.

Ndipo sindifuna kuti inu muyanjane ndi ziwanda. (1 Akorinto 10:20)

Simukuyenera kuchita ubale ndi aphunzitsi, atsogoleri, atumwi ndi aneneri onyenga:

Mupewe maonekedwe onse a coipa. (1 Atesalonika 5:22)

MUYENERA KULANKULA MOTSUTSANA NDI CHOIPA M'MAGOME

Okhulupirira sayenera kungoyang'anira choipa m'magome. Azibusa ayenera kulalika mau onse a Mulungu munthawi imene tikukumana ndi ziphunzitsp zonyenga (II Timoteyo 4:1-4). Chiphunzitso chonyenga ndi cha Satana ndipo chiyenera kubweretsedwa poyera. Ndipo okhulupirira sakuyenera kutenga gawo pa ntchito zakumidima. Koma iwo ayenera kuzibweretsa poyera ntchito ngati zimenezi(Aefeso5:11).

KUGWIRITSA NTCHITO UTUMIKI WA MAMASURIDWE:

Mpingo ngati chikonzero cha Mulungu ndi wamphamvu kuposa Satana. Taona kale kuti Yesu Khristu ndi mutu wa mpingo ndipo kuti okhulupirira ndi gawo la thupi la Khristu Yesu. Polingalira izi, werengani ma vesi ali munsiwa.

kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu, (Aefeso 3:10)

Yesu Khristu ndi mutu wa mpingo ndipo kuti okhulupirira ndi thupi la Khristu Yesu. Ndiye ngati zinthu zonse zili pansu pa mapazi a Khristu Yesu, chomwechonso zili pansu pamapazi athu chifukwa chakuti ife ndi thupi la Khristu Yesu. Mau oti pansu pamapazi akutanthauza kuti zonse zili pansu pa ulamuliro ndi mphamvu zimene Mulungu anatipatsa. Yesu anati wapereka mphamvu ndi ulamuliro onse kwa ife pa adani athu (Luka 10:19). Izi zikutanthauzanso kuti choipa m'magome chilonso pansu pa ulamuliro wathu.

Mpingo uyenera kuonetsera mpamvu pa maulamuliro ndi maukulu. Kotero, tiyenera kugwiritsa ntchito utumiki wa mamasilidwe ndi cholinga choti tikabweretse ufulu kwa onse amene ali mu goli la choipa chazimu m'magome am'mwamba. Tiyenera kubweza athu kuchokera kumdima wasatana ndi mphamvu yake ndi kuwatengera ku Ufumu wa Mulungu (Machitidwe 26:18)

KUYENDERA PERETE

1. Lembani vesi yotsogolera kuchokera mu zolembe zankhondo

2. Kodi magome am'mwamba amagwiritsidwa ntchito yotani?

3. Kodi mau oti choipa chauzimu m'magome am'mwamba ndi chiani?

4. fotokozerani mwachidule njira za choipa chauzimu zimene Satana amagwiritsa ntchito m'magome am'mwamba

5. fotokozerani mwachidule njira zimene tikhoza kugwiritsa ntchito pofuna kuthana ndi choipa m'magome am'mwamba?

(mayankho amafunso awa ali kumapeto kwaa buku ili)

MACHITACHITA A LUSO

1. Werengani machenjezo a Mulungu pa ana a Israeli okhudza Satana ndi zanyanga: Deteronome 18:10, Levitiko 12, 17:31; 20:16.
2. Werengani zambiri zokhudza nsembe zoperekedwa kwa Satana: Deteronome 32: 17: II Mbiri 11:15 ndi Salimo 106:37.
3. Ali mumsiwa ndi makhalidwe odziwika bwino lomwo azipembedzo zonyenga:
 - Amakhala ndi otsogoleri amphamvu okumva za iwo okha. Nthawi zambiri pamakhala munthu mmodzi kapena kagulu ka anthu kamene kamakhala ndi ndi mphamvu zambiri kuposa wina aliyense.
 - zipembedzo zonyenga nthawi zambiri zimakhala ndi mfundo zonena kuti iwo okha ndi amene ali ndi choonadi. Ndipo sayanjana ndi iwo amene sagwirizana ndi mfundo zao.
 - Zimakhala ndi mfundo zokhwima kwambiri zimene zilibe umboni ochejera mu Baibulo.
 - Nthawi zambiri iwo amaona ngati kuti boma kapena mabungwe ena cholinga chao ndi kutsutsana ndi iwo. Chifukwa cha ichi, nthawi zambiri iwo amakhala akudziyikira kumbuyo kapena kudzulura anthu ena.
 - Amakhala ndi nkhanza kwa anthu awo owatsatira. Izi amachita ndi atsogoleri.
 - Zochita zao zimakhala zachinsisi kwa anthu akunja.
 - Iwo amati analandira mavumbulutso kuchokera kwa Mulungu. Nthawi zambiri amakhala ndi zolembedwa zina zoonjezera Baibulo zimene amazitsatanso chimodzimodzi ndi Baibulo. Izi zimakhala zolembedwa mwina za atsogoleri awo zimene zimalembedwa pofuna kutanthauzira Baibulo.
 - Zikhulupiriro zao zimakhala zosemphana ndi Baibulo.
 - Nthawi zambiri iwo amakhala otsutsana ndi kayendetsedwa ka mpingo mwadongosolo kamene mipingo ina imatsata.
 - Nthawi zina iwo amatsutsana ndi anthu apabanja pawo pomwe. Izi zimathauza kuti amafuna kuti owatsatira awo athetse ubwenzi wao ndi abale awo amene samatsata chipembedzo chao.
4. Ndi zovuta kuti tithe kutchula chipembedzo chinachilichonse chonyenga chifukwa pali miyandamiyanda ya zipembedzo zimenezi. Koma pakadali pano, pali chipembedzo china chotchodwa” New Age Movement” chimene chikukula kwambiri. Tinaona kuti ndikofunika kuti titchule chiphunzitso cha ziwanda ngati chimenechi chifukwa pakadali pano, chipembedzo chimenechi chikukula kwambir makamaka mu dziko la United States of America. Nyumba zambiri zosindikiza mabuku pakadali pano zili ndi nthambi yoona zolembedwa za “New Age Movement.” Izi zili chomwechi chifukwa chakuti anthu ofuna kuwerenga zolemba zachipembedzo chimenechi akumka nachulukirabe. Koma chipembedzo chimenechi chiyambi chake ndi zamatsenga kapena za nyanga zimene zimachitika mayiko ngati Babulo. Dzina lakuti “New Age Movement” ndi latsopano

koma zamatsenga zimene zimachitika mkati mwachipembedzo chimenechi sizachilendo ayi.

Malingana ndi chipembedzo chimenechi, iwo amati Yesu ndi m' modzi mwa ovumbulutsa choonadi amene si osiyana ndi athu ngati Budda, Muhammad kapena Khrisha. Iwo amakana kuti Yesu ndi Mulungu. Ngakhale kuti munthu ndi otaika chifukwa cha tchimo, iwo amati munthu amabadwa wabwino. Iwo amaphunzitsa kuti munthu ndi olekanitsidwa ndi Mulungu chifukwa chachikumbumtima chake.

Chifukwa chachiphunzitso chakuti munthu ndi olekanitsidwa ndi Mulungu chifukwa cha chikumbumtima chake, chipembedzo cha “New Age Movoment” chimalimbikitsa zinthu monga ngati kulingalira mozama, kuvina ndi kugwiritsa ntchito mankhwala ndi cholinga chofuna kukonzaso chikumbumtima cha Munthu. Iwo amati pakuchita izi, ndiye kuti munthu apulumuka. Chifukwa cha mtchitidwe wa ufiti, nyanga ndi zithumwa, iwo amakhala kuti atsekula khomo ladziwanda mmoyo wao.

Chipembedzo chimenechi chimatsindika mfundo yoti munthu akafa amasanduka kukhala chinthu china. Iwo amati Satana wa munthu ndi mwina wake munthu komanso kuti munthu ndi mulungu wachipulumutso chake chomwe. Izi zikutanthauza kuti munthu ndi maziko achina chilichonse cha moyo wake. chimene munthu ayenera kuchita ndi kusankha chimene iye akuona kuti ndi cholondora kapena cholakwika. Chipembedzo chimenechi chimakana chikhalidwe chaugwiro wa Mulungu.

Iwo amakhulupirira kuti palibe chinthu chimene chili choipa. Chifukwa cha ichi, iwo amati palibe amene amakhudzika ndi umbava ndi Umbanda komanso. iwo amatinso imfe sichinthu chenicheni chifukwa chakuti munthu akafa amasanduka kukhala chinthu china. kotero palibe munthu amene ndi akhoza kukhudzidwa ndi imfa kapena kutaya mimba.

Zina mwa njira zimene chipembedzo cha “New Age Movoment” chikugwiritsa ntchito ndi kulowa mwakachetechede mumipingio imene yaima pa choonadi. Cholinga cha anthu amenewa akuti ndi kuyanjanitsa anthu onse. Kutu izi zitheke, iwo amakamba zakuchotsa anthu onse amene samadziona okha ngati mulungu. Pakadali pano ali pakalikiliki ofuna kubweretsa umodzi wadziko lonse lapansi. Koma umodzi umeneu ndi osalemekeza Mulungu chifukwa munthu ndi amene ali pamwamba pa china chilichonse. Izi zikuonetsera kuti chipembedzo cha “New Age Movement” ndi njira imodzi imene Satana akugwiritsa ntchito pofuna kuyanjanitsa dziko lonse lapansi komanso ndi bungwe limene anthu otsutsana ndi Khristu afuna kuligwiritsa ntchito kuti alamulire dziko lonse lapansi.

5. Werengani II Petro ndi Buku la Yuda. Tchulani chikhalidwe chimene chikhoza kukuthandizani kuti muzindikire anthenga a Satana mumpingo

Chikhalidwe cha aphunzits obodza

II Petro Chaputala cha 2
Aphunzitsi abodza amaphunzitsa chiphunzitso chonyenga: vesi 1
Amakana Ambuye Vesi 1
Tsopano pitirizani mdandanda umenewu:

Chikhalidwe cha anthu ena
amene alowa mumpingo mwachinsinsi.
Buku la Yuda

CHAPUTALA 21 KUTHANA NDI MPAMVU YA ZIWANDA

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili muyenera kukwanilitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kuzindikira mitundu ya ziwanda imene imagwira thupi, mzimu ndi moyo wa munthu.
- Kufotokozero kufunika kwa mphatso ya chidziwitso cha mizimu pothana ndi mphamvu yaziwanda.
- Kufotokozero tanthauzo logwida ndi chiwanda.
- Kuzindikira chikhalidwe cha munthu ogwida ndi ziwanda.
- Kufotokozero tanthauzo la kuzunzidwa ndi ziwanda.
- Kuzindikira makhalidwe amunthu ogwida ndi ziwanda.
- Kufotokozero mwachidule utumiki wa Yesu okhudzana ndi mphamvu ya ziwanda.
- Kugwiritsa ntchito ndondomeko za Baibulo pogonjetsa mphamvu yaziwanda

VESI YOTSOGOLERA YOCHOKERA MUZOLEMBA ZANKHONDO.

za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Macitidwe 10:38)

MAU OYAMBA

Kwa nthawi yaitali, ntchito za ziwanda zakhala zikutengedwa ngati mbali imodzi yachikhalidwe pakati pa anthu osakhulupirira. Anthu ambiri amaona ngati ili sivuto limene limasokoneza mabanja, mpingo ngakhale maiko kumene.

Monga mmene taonera kale, ziwanda ndi mphamvu za Satana zimene okhulupilira amalimbana nazo (Aefeso 6:12) Ziwanda ndi akezembe amene Satana amagwiritsa ntchito kuti akwaniritse zolinga zake pa dziko lapansi.

Chithunzi chili pansichi chikuonetsera zimene mwaphunzira za ziwanda komanso magawo amene zimagwira ntchito.

Mizimu yonyenga



Umalimbana ndi
mzimu wa munthu

mizimu yonyasa



umakhudza moyo wamunthu

mzimu wamatenda



umakhudza thupi la munthu



Mizimu iyi ikhoza:



Kuzuza munthu

Kugwira munthu

Kupangitsa chizolowezi chachikulu

Kuti muthe kumenya nkondo yoyenera, muyenera kudziwa njira zothana ndi mphamvu zaziwanda zimene zimagwira anthu, kubweretsa chizuzo kapena mizimu imene imabweretsa chizolowezi chosakhala bwino. Pali anthu ambiri amene akusautsika ndi ziwanda kapena amene anagwidwa ndi mphamvu yaziwanda. Chaputala ichi chifotokoza ndondomeko zimene zikhoza kugwiritsidwa ntchito potumikira anthu oterewa.

YESU NDI NDI ZIWANDA

Chiphunzitso ndi utumiki wa Yesu Khristu zinaonetsera kuti ziwanda ndi mphamvu ya choipa. Zimene Yesu anaphunzitsa zokhudza ziwanda komanso mmene iye anachitira ndi ziwanda, zimaonetsera njira zimene Satana amagwiritsa ntchito.

Yesu Khristu amazindikira kuti Satana ndi olamulira wachikhamu chaziwanda. Iye anaphunzitsa za mphamvu ndi kupezeka kwa ziwanda. Iye anafotokozerera kuti kuchotsa ziwanda ndi chizindikiro chimodzi choti ufumu wa Mulungu wafika. Werengani ndime izi: Mateyu 12:22-30, Marko 3:22-27, ndi Luka 11:14-23. Ndime zimenezi zikuonetsera mwachidule zimene Yesu anaphunzitsa zokhudza ziwanda.

Kulimba ndi ziwanda linali gawo lalikulu la utumiki wa Yesu Akhristu. Ulamuliro umene dzina la Yesu linali nawo ndi umboni okwanira opezeka mu Baibulo kuti tiyenera kuthana ndi ziwanda. Yesu anatomikira kwa nthu onse amene anabwera kwa iye ndi vuto laziwanda. Petro anati kwa Yesu:

za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Macitidwe 10:38)

Mu gawo la zoonjezera pophunzira, tiona zitsanzo zokhudza ziwanda zimene Yesu anachitapo kanthu.

KODI ZIWANDA ZIMAGWIRA NTCHITO BWANJI?

Monga mmene taonera kale, ziwanda zimagwiritsidwa ntchito ndi Satana kuti zitsutsane ndi zolinga ndi chikonzero cha Mulungu komanso kuti zikatsutsane ndi anthu ake a Mulungu. Zimalimbananso ndi anthu osakhulupirira kuti asazindikire choonadi chauthenga Wabwino. Pali madera ena amene amalamuliridwa ndi mizimu yoipa. Mwachitsanzo, buku la Danieli limatchula karonga olamulira dera la Peresiya (Danieli 10:12-13). ziwanda zimagwira ntchito kudzera mwa amayi ndi abambo pofuna kukwaniritsa zolinga za Satana pa dziko lapansi.

Kutsutsana ndi chifuniro cha Mulungu ndi cholinga chenicheni cha Satana. Mau oti Satana amathanauza kuti mdani. Ndipo mdani wamkhulu wa Mulungu ndiye Satana (Yobu 1:6; Mateyu 13:39). Mdani wake wachiwiri ndi munthu (Zakariya 3:1; I Petro 5:8).

Taona kale muphunziro lina kuti ziwanda zili ndi chikhalidwe chosiyanasiya. Mwachitsanzo, chiwanda china chinadzitchula chokha dzina kuti icho ndi “mzimu wabodza” (I Mafumu 22:23). Mzimu osamva ndi osalankhula ukutchulidwanso pa Marko 9:25. Pali ziwanda zamitundu yosiyanasiya zimene zimagwira ntchito ngati mizimu yosiyanasiananso. Ina mwamizimu imeneyi ndi mizimu yonsansa komanso mzimu oyenga. Satana amagwiritsa ntchito mizimu imeneyi kuti achite nkondo yolimbana ndi thupi, moyo ndi mzimu wa munthu.

MIZIMU YAMATENDA

Iyi ndi mizimu imene imalimbana ndi thupi la anthu okhulupirira ndi osakhulupirira omwe. Werengani Luka 13:10-17. Mzimayi ameneyu anagwidwa ndi mzimu wamatenda. Iye anapita kukapembedza pa tsiku la Sabata pamene Yesu anaitana iye nati “mwana mwa Abrahamu.” Izi zikutanthauza kuti iye anali munthu okhulupirira Mulungu ngakhale thupi lake linazuzidwa ndi Satana kwa zaka makumi asanu ndi zitatu. Mukhoza kuwerenga Mateyu 12:22; 17:15-18; Machitidwe 10:38; II Akorinto 12:7 kuti muone zitsanzo zina zaziwanda zikuzunza nthupi la munthu.

MIZIMU YONYENGA:

Mizimu imeneyi imalimbana ndi mzimu wa munthu. Cholinga cha mizimu imeneyi ndi kunyenga munthu kuti akhulupirire chikhulupiriro chabodza ndi cholinga choti akalangidwe ndi chilango chosatha. Iyi ndi mizimu ya chiphunzitsa chonyenga, zipembedzo zonyenga komanso aphunzitsi onyenga.

Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m' masiku otsiriza ena adzataya cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunziro a ziwanda, (1 Timoteo 4:1)

Koma iyi ndi mizimu yachinyengo imene imachita zozwizwitsa. Chifukwa cha ichi, ena amakhulupirira kuti ndi yochokera kwa Mulungu.

pakuti ali mizimu ya ziwanda zakucita zizindikilo; zimene zituruka kumka kwa mafumu a dziko lonse, kuwasonkhanitsira ku nkondo ya tsiku lalikuru la Mulungu, Wamphamvuyonse. (Cibvumbulutso 16:14)

ndiye amene kudza kwace kuli monga mwa macitidwe a Satana, mu mphamvu yonse, ndi zizindikilo ndi zozizwa zonama; ndi m'cinyengo conse ca cosalungama kwa iwo akuonongeka, popeza cikondi ca coonadi sanacisandira, kuti akapulumsidwe iwo. (2 Atesalonika 2:9-10)

Mizimu yanyanga ndi gawo limodzi la mizimu yonyenga imene yatchulidwa mu buku la Machitidwe:

Ndipo panali, pamene tinalinkunka kukapemphera, anakomana ndi ife namwali wina amene anali ndi mzimu wambwebwe, amene anapindulira ambuye ace zambiri pakubwebweta pace. (Macitidwe 16:16)

Mizimu yanyanga imaonekera kudzera mwa anthu onenera mwayi, afiti ndi ena onse amatsenga. Pogwiritsa ntchito njira zimene ndi zosempana ndi Baibulo, mizimu ya nyanga imatha kunenera za mtsogolo zimene munthu pa umunthu wake sangathe kuzidziwa. Koma machenjezo okhudzana ndi mizimu imeneyo aperekedwa pa Levitiko 19:31; 20:6; Deteronome 5:9; 18:10, Levitiko 20:27 ndi I Samueli 28:3.

Mizimu yonyenga imakomedwetsa, imakopa, imabweretsa chiyeso komanso imapha chikumbu mtima. Iyi ndi mizimu imene imagwira ntchito malo ena ali onse amene pali chiphunzitsa chonyenga komanso onse amene pali choipa chazimu m'magome am'mwamba amene akambidwa mu chaputala 20.

MIZIMU YONYANSA:

Iyi ndi mphamvu yaziwanda imene imagwira moyo wa munthu. Iyi ndi mizimu imene imapangitsa anthu kuchita makhalidwe onyansa kapena osayenera, maganizo onyansa, mayesero ndi njira zina zimene Satana amagwiritsa ntchito pofuna kumanga anthu mugoli. Pamene Satana akulamulira anthu ndi mizimu yonyansa, iye amakhala kuti akugwira ntchito malo osiyanasiyana chifukwa chakuti malo ena alionse amakhala ndi anthu amene akhoza kugwidwa ndi mizimu imeneyi. Werengani ndime izi kuti muone zitsanzo za mizimu yonyansa Mateyu 10:1; 12:43; ndi Marko 1:23-26.

KUZUZIDWA, KUGWIDWA NDIKUPEREKA CHIZOLOWEZI CHACHIKULU

Mizimu yoipa imatha kuzunza anthu. Kuzunza kumatanthauza kuchita motsutsana ndi wina, kapena kumanga chinthu kunja kwakwe. Mizimu yoipa imakwaniritsa kuzunza anthu pogwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana. Mwachitsanzo, mizimu yoipa imatha kubweretsa nkhwana, kubweretsa nyengo zowawitsa, kubweretsa maganizo olakwika monga maganizo ofuna kudzipha

wekha, chisawawa, mantha ndi zina zambiri. Ziwanda zimabweretsa mayesero pa munthu ndi cholinga choti munthuyo achimwe.

Za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Macitidwe 10:38)

Anthu amathanso kugwidwa ndi ziwanda. Izi zimatanthauza kuti ziwandazo zapeza malo nthupi la munthu ndikuyamba kulamulira moyo wa munthuyo malinga ndi mmene zikufunira. Koma kugwidwa ndi ziwanda sizitanthauza kuti munthu alibe udindo pa zochimwa zake. Izi zili chomwechi chifukwa pamakhala kuti pali chinthu chimene chimayambitsa kuti munthu agwidwe ndi dziwanda.

Munthu akhoza kugwida ndi ziwanda chifukwa chakuti wachita kufuna. Ena amatha kusankha kutero pofuna kukhala mfiti, kukhala ndi mphamvu zapadera kapena kuti adzitha kutembelera anthu ena. Munthu akhoza kugwida ndi mizimu osati chifukwa chakuti wafuna, koma chifukwa cha maganizo kapena zochita zauchimo, zimatha kupangitsa munthu kuti agwide ndi ziwanda.

Mphamvu yaziwanda imene imagwira ntchito mwa makolo imatha kukhudza ana. Werengani ndime izi: Ekisodo 20:5; 34:7; and Deteronome 5:9.) Izi zikuonetsera kugwidwa ndi ziwanda pakati pa ana ngati mmene aonetsera pa Marko 7:24-30 and 9:17-21.

Pali anthu ena amene amakhala ndi chidwi chachikulu ndi dziwanda. Anthu oterewa amaonetsera chidwi chachikulu ndi ziwanda, nyanga komanso ndi Satana amene amatha kuyamba kulamulira moyo wao. Chidwi chachikulu ndi ziwanda chikhoza kupangitsa kuti munthu agwidwe ndi ziwandazo.

KODI OKHUPIRIRA AKHOZA KUKHUDZIDWA NDI ZIWANDA?

Okhulupirira weniweni sangagwidwe ndi ziwanda chifukwa Mzimu Woyera sangagonera malo amodzi ndi kachisi wa mzimu oipa.

Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha. Pakuti munagulidwa ndi mtengo wace wapatali; cifukwa cace lemekezani Mulungu m'thupi lanu. (1 Akorinto 6:19-20)

Ngati muli okhulupirira odzadzidwa ndi Mzimu Woyera, ndi zosatheka kuti mukhale wake wa Satana komanso odzadzidwa ndi mizimu yake. Mzimu wayera sangakhalire malo amodzi ndi kachisi wa Satana.

Koma izi sizikutanthauza kuti anthu okhulupirira sangakhudzidwe ndi mphamvu yaziwanda. Izi zili chonchi chifukwa mphamvu zimene timalimbana nazo ndi za Satana. Satana amagwiritsa ntchito ziwanda pofuna kulimbana ndi okhulupirira, koma ndi zosatheka kuti okhulupirira

weniweni kuti akhoza kukhudzidwa. Kugwidwa ndi ziwanda zimanthauza kuti mizimu yoipa yakhazikika mkati mwa munthu. Pamene timakamba nkhani ya kuzuzidwa kapena kumangidwa ndi ziwanda, zimaonetsera kuti ziwandazo zikugwira ntchito kuchokera kunja kwa munthu. Zochitika za anthu okhulupirira zikhoza kukhudzidwa ngati iwo amulora Satana kuti awazunze ndi kumulora kuti awagwiritse ntchito pokwaniritsa zolinga zake.

Izi ndi zimene zinachitika ndi Petro, otsatira wa Yesu. Iye anagwiritsidwa ntchito ndi Satana pofuna kuletsa Yesu Khristu kuti asakwaniritse cholinga chake chofuna kufera anthu onse. Yesu atafotokoza za chizuzo chimene amayenera kudutsamo, Petro anati:

Ndipo Petro anamtenga Iye, nayamba kumdzudzula, kuti, Dzicitireni cifundo, Ambuye; sicidzatero kwa Inu ai. (Mateyu 16:22)

Yesu anati kwa Petro:

... Pita kumbuyo kwanga, Satana iwe; ndiwe condikhumudwitsa Ine; cifukwa sumasamalira za Mulungu, koma za anthu. (Mateyu 16:23,)

Sikuti Yesu amatanthauza kuti Petro ndi Satana. Koma iye amazindikira kuti Satana anali atalowa ndikuyamba kugwira ntchito mwa Petro. Petro sanagwidwe ndi ziwanda koma iye analora kuti mizimu yoipa imugwiritse ntchito iye.

ndiponso musampatse malo mdierekezi. (Aefeso 4:27)

Pamene munthu wabadwa mwatsopano, dzina lake limalembedwa mu Buku lamoyo kumwamba. Koma ndi okhao amene dzina lao linalembedwa mu buku lamoyo amene adzakhale ndi Mulungu kwa muyaya.

Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m'buku la moyo, anaponyedwa m'nyanja yamoto. (Cibvumbulutso 20:15)

Ndizotheka kuti dzina lanu likhoza kulembedwa mu mubuku lamoyo. Koma likhoza kifufutidwanso chifukwa chobwelera ku moyo wa uchimwa:

Iye amene alakika adzambveka motero zobvala zoyera; ndipo sindidzafafaniza ndithu dzina lace m'buku la moyo, ndipo ndidzambvomereza dzina lace pamaso pa Atate wanga, ndi pamaso pa angelo ace. (Cibvumbulutso 3:5)

Koma ngati okhulupirira apitilira kukhala moyo osalapa tchimo lodziwika, imafika nthawi imene munthu amasiya kukhala okhulupirira. Mtumwi Paulo akufotokoza nkhwawa yake kuti atalalikira uthenga wabwino angadzayambe kuchotsedwa;

koma ndipumpuatha thupi langa, ndipo ndiliyesa kapolo; kuti, kapena ngakhale nditalalikira kwa ena, 5 ndingakhale votayika ndekha. (1 Akorinto 9:27)

Paulo amazindikira kuti machimo akuthupi osalapidwa akanatha kumpangitsa iye kuti ataye moyo wake atatha kulalikira anthu ena.

Ngati munthu apitirira kukhala moyo wauchimo, mathero ake amakhala kugwa. Izi zimatanthauza kuti munthuyo siotsatiranso wa Yesu Khristu. Ngati munthu apitirira kukhala m'machimo osalapa, palibe amene angamuuze munthuyo pamene amasiya kukhala okhulupirira wa Yesu Khristu. Ndi Mulungu yekha amadziwa izi. Koma pamene izi zachitika, zimakhala kuti mwatsekula mabowo amene Satana akhoza kulowerapo. Ichi ndi chifukwa chake ndi kofunika kuti pamene mwachimwa, muyenera kulapa mwachangu ndi zonse zosalungama.

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. Tikanena kutisitidacimwa, timuyesa iye wonama, ndipo mau ace sakhala mwa ife. (1 Yohane 1:9-10)

Baibulo limamufotokoza Yesu Khristu ngati Mau a Mulungu. Ndiye ngati mau a Mulungu Sali mkati mwanu, ndiye kuti mkati mwanunso mulibe Yesu.

KODI ZIWANDA ZIMATENGA BWANJI ULAMULIRO?

Ziwanda zimatenga ulamuliro pogwiritsa ntchito njira izi:

1. Kudzera mumibado: ziwanda zimamatha kumuzuza munthu kapena kumugwira kumene chifukwa cha makolo. Ichi ndi chifukwa chake ana amatha kukhudzidwa ndi mphamvu yaziwanda (Ekiisodo20:5; 34:7; Deteronome 5:9).
2. Kudzera mumaganizo: Maganizo ndi gawo limodzi limene Satana amalimbana nalo. Ngati Satana amalamulira maganizo anu, mapeto ake amathanso kulamulira zochita zanu. Kulephera kuyang'anira maganizo anu kukhoza kupangitsa kuti mudzikanika kupanga ziganizo panokha. Ngati zotsatira za izi, mumayamba kuchita zinthu zauchimo ndipo izi zimapangitsa kuti mugwidwe kapena kuzunzidwa ndi ziwanda. Mapeto ake mukhala ndi mtima opanda chikumbumtima chilichonse ngati mmene akufotokozerera pa Aroma 1. ziwanda zimathanso kulowa mwa munthu chifukwa chogwiritsa ntchito mankhwala ozunguza ubongo. Izi zimachepetsa kuthekera kwa munthu kotsutsana ndi ziwanda kotere kuto zimapezerapo mwayi olova mwa munthu.
3. Zochita zauchimo: Maganizo auchimo amasanduka ndikukhala zochita zauchimo. Mwachitsanzo, maganizo achigololo amakwanilitsidwa pakuchita chigololo. Tchimo ndi kuukira kotera kuti zochita zoukira zimapereka danga kuti ziwanda zilowe mwa munthu. Kwa anthu osakhulupirira amene amakhala muuchimo, kumakhala kosavuta kuti agwidwe komanso kuzuzidwa ndi ziwanda. Tinaona kale kuti palibe munthu amene angakhale pakatipakati ikafika nkhani ya nkondo yauzim. Munthu amakhala mbali ya Satana kapena ya Mulungu. Ngati inuyo muli wake wa Satana ndipo simunabadwe mwatsopano, Satana akhodza kukugwiritsani ntchito monga mmene akufunira.

4. Kudzera muzilakolako: Anthu ena amachita kupempha kapena kufuna kuti akhale pansa pa Satana. Iwo amachita izi ndi cholinga choti akhale ndikuthekera kopanga zinthu zodabwitsa.
5. Kudzera “nyumba” yopanda kathu: Ziwanda zimatenga thupi la munthu amene zimakhalamo ngati nyumba yawo. (Mateyu: 12:44) Pamene munthu wabadwa mwatsopano ndipo ngati nyumba yake sidzadzidwa ndi Mzimu woyera, ndiye kuti amakhala kuti wapereka danga kuti nyumba yake ilowendwenso.
6. Popereka chilolezo: Nthawi zina Mulungu amatha kulora ntchito za ziwanda kuti zitifikire ndi cholinga choti akwaniritse zolinga zina zapadera. Chitsanzo chabwino ndi Yobu. Koma izi zikhoza kuchitika ngati zotsatira zauchimo. Saulo ndi chitsanzo chabwino cha zimenezi.

KODI NDI NDANI AMENE AYENERA KULIMBANA NDI MPHAMVU YAZIDZIWANDA?

Kulimbana ndi ziwanda si udindo wa abusa okha ayi. Yesu Khristu anafotokoza kuti okhulupirira adzakhala ndi mphamvu zogonjetsa mphamvu yaziwanda.

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; (Marko 16:17)

Yesu anapereka kuthekera kothana ndi mphamvu yaziwanda kwa ophunzira ake onse. Pachiyambi, iye anapereka mphamvu imeneyi kwa ophunzira ake:

Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi yakuciza nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 10:1)

Ndipo anadziitanira khumi ndi awiriwo, nayamba kuwatumiza Iwo awiri awiri; nawapatsa mphamvu pa mizimu yonyansa; (Marko 6:7)

Palibe umboni opezeka mu Baibulo kuti ntchito yolimbana ndi ziwanda ndi ya anthu ochepe chabe. Munthu wamba dzina lake Filipo anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kuchotsa ziwanda ku dera la Samariya. Koma izi sizikuthandauza kuti okhulupirira ayenera kuchita machawi ndi kuyamba kulimbana ndi ziwanda asanakonzekere mokwanira, ngati mmene anachitira ana a skeva (Machitidwe 19)

Ndi zofunika kwambiri kuti okhulupirira asakhazikike paziwanda. Izi chili choncho chifukwa sitinayitanidwe kuti tingokhazikika pa ziwanda. Palibe mpatso yochotsa ziwanda. Koma inu simukuyenera kuopa ziwanda ndipo pamene mwakumana ndi iwo amene agwidwa kapena kuzunzidwa ndi ziwanda, muyenera kukhala ndi kuthekera koti iwo amasulidwe ndi Mulungu.

KIZINDIKIRA KUPEZEKA KWA DZIWANDA

Kuti muthu athe kugonjetsa mphamvu yaziwanda ndi zofunika kuti kuzindikira kupezeka kwake komanso njira zimene zimagwiritsa ntchito. Mzimu Woyera amapereka mphatso yapadera yothandizira kuzindikira kupezeka kwa ziwanda. Mphatso imeneyi imatchedwa mphatso yachidziwitso (I Akorinto 12:10)

Mphatso yachidziwitso imathandiza okhulupirira kuti athe kuzindikira mizimu imene ikugwira ntchito mwa anthu ena. Mphatso imeneyi umathandiza kuti mukathe kuzindikira ngati munthu ali ndi mzimu oipa kapena ayi. Mphatsoyi imathandizanso kupewa kunamizidwa ndi mizimu yonyenga. Munthu amene ali ndi mphatso imeneyi akhoza kuzindikira njira za ziwanda komanso mphamvu yake.

Malingana ndi Baibulo, matenda ena osamva ndi kulankula amayamba chifukwa cha mizimu yoipa. Pamene kusamva kwina ndi kusalankhula ndi zotsatira zamatenda kapena ngozi. Mphatso yachidziwitso imathandiza kuti muzindikire choyambitsa chenicheni cha zinthu ndipo izi zimathandiza kuti mupange chiganizo choyenelera.

Mzimayi wina anabwera kwa Yesu napempha iye kuti achotse mzimu onyansa pa mwana wake wamkazi. Mzimayiyu anazindikira vuto la mwana wake chifukwa cha zizindikira zimene mwanayo amaonetsa (Mateyu 15:22). Kuzindikira chiwanda kumatengera kuyang'anira zimene chiwandacho chikuchita kwa munthuyo.

Zina mwazizindikiro za zochita zaziwanda ndi izi:

Kukhala ndi chidwi chachikulu ndi ziwanda: Izi zimaonekera pamene munthu ali ndi chidwi chachikulu ndi Satana, zanyanga ndi ziwanda. Anthu oterewa amatha kuyamba kuyesa zanyanga, kuombeza kuti awone kuti zinthu zikuchitika chifukwa cha Satana kape ziwanda. Komanso anthu oterewa amatha kuononga nthawi yawo yambiri kuphunzira ndi kuwerenga zinthu zokhudza ziwanda ndi Satana.

1. Kuzuzidwa ndi dziwaanda: Izi zikhoza kuzindikiridwa ndi zizindikiro izi:

Kumangidwa kuthupi “mwana wamkazi a Abrahahamu amene Yesu anam’masula ku mzimu wamatenda anali atamangidwa kuthupi. Werengani Luka 13: 10-17. Nthawi zina matenda amgonagona amabwera chifukwa cha dziwanda. Pamene matenda ena amabwera chifukwa chosatsata dongosolo lachilengedwe. Mwachitsanzo munthu akhoza kudwala chifukwa chakudya mosayenera kapena kumwa madzi osakhala bwino. Pamene matenda ena amabwera ngati chilango. Mfumu ina mu Baibulo inamwalira ndi njoka za m’ mimba chifukwa chifukwa chosalemekeza Mulungu.

2. Kuzunzidwa m’ maganizo: Izi zikhoza kuonekera kudzera mu zinthu ngati kusokonekera m’ maganizo, kuyiwala zinthu, kusakhazikika malo amodzi, kusatha kumvetsera zimene anthu ena akunena. Nthawi zina munthu amalankhula kwambiri modabwitsa kepana kukhala chete kwambiri. Izi sizikutanthauza kuti matenda am’bongo amayamba chifukwa cha Satana.

Nthawi zina matendawa amatha kuyamba chifukwa cha Satana. Matenda amenewa akhozanso kubwera chifukwa cha zinthu ngati, chakudya chosayenera kapena chifukwa cha nkhwawa. Koma Mulungu amatha kuchiritsa matenda onsewa kaya oyamba chifukwa cha mphamvu ya ziwanda kapena ayi. Payenera kusamalitsa chifukwa zikhoza kutheka kumaona matenda am'bongo ngati chizindikiro cha ziwanda. Nthawi zina kungosintha kakhalidwe komanso kadyedwe kamatha kuthetsa vuto la matenda a m'bongo ngati vutolo linayamba pazinthu zachilengedwe.

3. Nkhawa: kuchita nkhwawa kawirikawiri kukhoza kubweretsa zinthu ngati izi: mkwiyo, mantha, kudzimvera chisoni wekha, kudandaula ndi zina zambiri.
4. Mavuto azauzimu: zina mwa izi ndi kuvutika kwambiri kugonjetsa tchimo, kukhala ndi chizolowezi cha tchimo. Kukana mayankho auzimu amavuto athu. Chiphunzitsa china chilichonse chonyenga kapena kukhala mu goli ndi zinthu zazipembedzo zonyenga makakamaka zolembe zao.
5. Nyengo zanu: ziwanda dzikhoza kubweretsa nyengo zowawitsa pamoyo wanu. Nyengo zimenezi zimabweretsa chisokonezo ndipo mukhoza kuzizindikira kuti ndi za Satana chifukwa Mulungu sabweretsa chisokonezo (1 Akorinto 14:33 ndi Yakobo 3:16)

Kugwida ndi ziwanda kukhoza kuzindikiridwa ndi zizindikiro izi:

1. Kukhala ndi mizimu yonyansa: Izi zimaokera kudzera mukhalidwe lonyansa limene munthu amaonetsa. Mwachitsanzo, ene amatha kufuna kuyend opanda chovala werengani Marko 5:2 ndi Luka 8:27.
2. Mphamvu zambiri zachilendo: Munthu amaonetsera mphamvu zoposa zachilengedwe. Werengani Marko 5:3 ndu Luka 8:29.
3. Kudzambatuka ndi mkwiyo: izi zimayendera limodzi ndi thovu kukamwa. Werengani Marko 9:14-29 ndi Luka 8:26-39.
4. Kutsutsana ndi zinthu zauzimu: Malingana ndi Marko 6:7 ndi 1:21, ziwanda zinamuzindikira Yesu ndipo zinapempha kuti azisiye. Kuopa dzina la Yesu, mapemphero, komanso kulankula mau onyoza Mulungu ndi chizindikiro chogwida ndi ziwanda. Nthawi zina anthu amenewa amasintha machitidwe pamene zinthu za Mulungu zatchulidwa.
5. Khalidwe limasintha. Anthu amenewa ndi amanyazi ndipo amatha kuyamba kuchita chipolowe. Zochita ngakhale maonekedwa amene amathanso kusintha. Mau a munthu amatha kusintha. Werengani Marko 5:9.
6. Munthu amasautsika kuthupi. Pamene munthu wagwida ndi mizimu yoipa, thupi lake limatha kuyamba kuonda. Werengani ndime izi (Mateyu 9:33; 12:22; Marko 5:4-5, 9:14-29).
7. Kudzivulaza wekha. Pa Mateyu 17:14-21, pali nkhani ya Mzibambo wina amene mwana wake anadziponya pamoto (Luke 8:26-39). Munthu ameneyu amadzivulaza yekha podzicheka ndi mwala.

8. Kusautsika: Luka 8:28 amafotokoza nkhani ya munthu wina amene amafuula chifukwa chakusautsika mkati mwake ndi ziwanda.
9. Kukanika kukhala ndi anthu ena: Munthu ameneyu amakanika kukhala ndi anthu ena koma iye amakhala kumanda. Werengani Luka 8:27
10. Pogwiritsa ntchito njira zosemphana ndi Baibulo, anthu amenewa amatha kulosera zinthu zam'tsogolo kapena kutha kuzindikira zinthu zimene anthu ena sakuzidziwa. Mzimayi amene akupezeka pa machitidwe 16:16 anagwida ndi mzimu obwebweta.

Zina mwa zinthu zimene zimatha kuonetsera kugwida kapena kuzuzidwa ndi ziwanda ndi izi:

1. Chizolowezi cha chikhalidwe choipa monga kuonera kanema olaura, chigololo, dama, mathanyula ndi machimo ena okhudza kugonana. Kukhala ndi chilakolako chachikulu chofuna kudya chakudya, kudzicheka thupi komanso maganizo ofuna kupha.
2. Kumwa mowa mwauchidakwa ndi kugwiritsa ntchito mankhwala ozunguza ubongo.
3. Masomphenya komanso kuganiza zinthu zosagwirizana ndi Mulungu.
4. Kukhala mugoli la mantha, nkhwawa, nkwiyo nsanje komanso miseche.

NJIRA ZOLIMBANIRA NDI ZIWANDA

Zina mwa njira zothana ndi mphamvu ya ziwanda malingana ndi Baibulo ndi izi:

KUDZIKONZEKERETSA NOKHA.

Chikhulupiriro chimadza kudzera mu kumva mau a Mulungu. Mau a Mulungu olembedwa amakuza chikhulupiriro mkati mwanu. Izi zimachitika ngati mungawerenge chipangano chatsopano ndi maonedwe atsopano:

- Chilichonse chimene Yesu anauza ophunzira ake.
- Chilichonse chimene analonjeza kuti adzachita, muyenera kuyembekezera kuti azichita.
- Ngati analonjeza kuti adzalanditsa onse osautsidwa ndi Satana, chomwecho muyenera kuyembekezera kuti Iye akumasulani.
- Ngati ananena kuti mudzachotsa ziwanda, chomwecho muyenera kuyembekezera kuti ziwanda ziyenera kukumverani inu.

Simukuyenera kuyang'anira ziphunzitso za anthu ena kapena zinthu zimene mwakhala mukukumana nazo. Muyenera kukhulupirira zimene Chipangano Chatsopano chimakamba kuti ndi choonadi chenicheni. Inuyo ndi Kazembe wa Khristu Yesu (II Akorinto 5:20). Kazembe samakhala ndi chikaiko china chilichonse ndi dziko limene akutumikira.

Muyenera kupephera ndi kusala kudya ngati mukufuna kuchita mamasulidwe. Polingalira kuti mphamvu yamamasulidwe imachokera kwa Mulungu, ndi zofunika kuti mukhale olumikizana ndi Mulungu. ziwanda zina zimatuluka pokhapokha ngati pali pemphero ndi kusala kudya. Pa

Yesaya 58, amaphunzitsa kuti, Mulungu amalemekeza kusala kudya kumene kumachitika chifukwa cha zosowa za anthu ena.

KUKONZEKERA NDI ANTHU ENA:

Ngati kuli kotheka, ndi bwino kukhala guru la anthu okhulupirira pamene mukufuna kuchotsa ziwanda. Yesu amatumiza ophunzira ake mumagulu kuti akachite utumiki.

Ndipo anadziitanira khumi ndi awiriwo, nayamba kuwatumiza Iwo awiri awiri; nawapatsa mphamvu pa mizimu yonyansa; (Marko 6:7)

Izi sizikutanthauza kuti simungatumikire pa inu nokha mutakumana ndi munthu amene akufunika mamasulidwe. Koma nkhani ndi yakuti, muli mphamvu pamene anthu apemphera ngati gulu apemphera pamodzi. Chifukwa chakuti mphamvu zimachokera mu umodzi, ndi zofunika kwambiri kuti amene akufuna kuchita nanu utumiki wa mamasulidwe ayenera kukonzekera mupemphero ndi kusala kudya ngati mmene m'machitira inuyo.

Ngati munthu amene mukufuna kumtumikirayo ndi ogwida kapena kuzinzidwa ndi ziwanda, munthuyo ayenera kukonzekeretsedwa. Chikhulupiriro chao chiyenera kukunzidwa pogwiritsa ntchito Mau a Mulungu olembedwa. (koma izi zikhoza kukhala zovuta kwa munthu amene wagwida ndi ziwanda)

Ngati mungamulimbikitse munthu amene wagwidwa ndi ziwanda kuti amasulidwe, zili ngati kulimbikitsa munthu amene sanapulumutsidwe kuti alandire Yesu asanadziwe kuti Yesu ndi ndani, komanso asanavomereze machimo awo ndikuzindikira kuti akufunika mpulumutsi. Pamene mukulalika uthenga wabwino, ndi chinthu chanzeru osapanga chiganizo mofulumira. Pamakhala kufunika kochita utumiki wapadera, munthuyo ayenera kuphunzitsidwa bwino asanapange chiganizo.

Chimodzimodzi ndi mamasulidwe, payenera kukhala dongosolo lapadera limene lafotokozeredwa pamwambapali. Tiyenera kudziwa kuti Mulungu amamasula anthu opanda dongolo latchulidwali. Komabe ndi zofunika kuti pamene mukufuna kuchita utumiki wamamasulidwe, muyenera kutsata njira zoyenera zimene mau a Mulungu amafotokoza. Pozindikira kuti chikhulupiriro ndi njira imene Mulungu amagwiritsa ntchito, ndi zofunika kuti munthu ofuna kumasulidwa uja aphunzitsidwe, chifukwa chikhulupiriro chimadza pakumva mau. Yesua ali kuphunzitsa, kulalika, kuchilitsa ndi kumasula anthu kumphamvu yaziwanda mu utumiki wake. Chomwechonso anauza ophunzira ake kuti achite mmene iye amachitira.

MALO OCHITIRA UTUMIKI

Utumiki wa mamasulidwe uyenera kuchitika nthawi imene chipembedzo chikuchitika. Izi zili chomwechi chifukwa utumiki umeneu ndi gawo limodzi la utumiki wa mpingo choncho sikoyenera kuti nthawi zonse udzichitika nseri ndi anthu okhudzidwawo.

Yesu anatumikira anthu ogwidwa ndi ziwanda munthawi yopemphera mukachisi (Marko 1:21-25). Koma izi sizikutanthauza kuti muyenera kudikira nthawi yachipembedzo kuti muchite utumiki wa mamasuridwe. Yesu anali kumasura onse aziwanda amene amakumana nawo.

NTHAWI YAUTUMIKI:

Pamene mwakonzeka kuti muchitie utumiki wa mamasuridwe...

1. Yambani ndi matamando ndi mayamiko:

Kudzera mumatamando ndi mayamiko, timalowa mukupezeka kwa Mulungu (makamaka pamene pali machiritso ndi mamasulidwe) Mamasulidwe ndi machilitso amatha kubwera kudzera mu matamando ndi mayamiko. Ngakhale popanda pempero, athu amatha kumasulidwa chifukwa Mulungu amalemekeza matamando ndi mayamiko a anthu Ake. Pamene tiyamika Mulungu, kupezeka kwake kumatha kuchiritisa.

2. **MUYENERA KUKHAZIKITSA CHIKHULUPIRO.**

Mumakhala kuti mwayamba kale kukhazikitsa chikhupiro kudzera mu kuphunzitsa kwa mau okhudza mamasulidwe. Koma mukhozabe kuchitabe zinthu zina pofuna kukuza chikhulupiro. Kupanda chikhulupiro kunakhudza ngakhale utumiki wa Yesu Khristu ku Nazareti. Nthawi zina Yesu amathamangitsa anthu osakhulupirira pamene akufuna kuchita mamasulidwe (Marko 5:35-40). Nthawi zina amatuluka nawo anthu aja m'mamidzi awo ndi cholinga choti awatumikire. (Marko 8:23). Mwina nthawi zina pamene mukutumikira, muyenera kupempha anthu amene ali ndi mantha kapena opanda chikhulupiro kuti achoke.

3. Pempherani ngati chinthu choyamba:

Muyenera kupemphelera chidziwitso ndi nzeru pamene mukufuna kuchita utumika wa mamasulidwe. Pamene mukupemphera, Mulungu akhoza kukuonetserani zinthu izi:

- Mau achidziwitso: Mulungu akhoza kukuonetserani mmene nyengo ya munthuyo iliri ndipo izi zimathandizira kuti mudziwe mapempheredwe ake. Mau a chidziwitso akhoza kuonetsera chimene munthuyo akudwala komanso chimene chinayambitsa matendawo.
- Mulungu akhoza kuonetseranso Mau ake olembedwa mu Baibulo ogwirizana ndi nyengo ya munthuyo.
- Mulungu akhoza kupereka masomphenya kapena kuti chithuzithunzi cha munthu amene mukumtumikirayo.
- Kudzodza kwapadera. Mukhoza kulandira mphamvu yapadera pamene mukupephera.

4. **CHEZANI NAYE MUNTHUYO KWA NTHAWI YOCHEPA**

Ichi sichokakamiza choncho muyenera kuchita malingana ndi mmene Mulungu wakuyankulirani. Koma Mulungu ankhoza kukupatsana mau achidziwitso okhudza munthuyo. Chifukwa cha ichi sikoyeneranso kukhala naye pansu munthuyo kuti mumve kuchokera kwa iye.

Koma ngati simulandire chidziwitso chilichonse kucholera kwa Mulungu, musazengereze kucheza naye munthuyo kuti mudziwe zinthu zina. Yesu amatha kugwiritsa njira zakuthupi ndi zauzimu zomwe. Munyengo zina iye amadziwa nyengo imene munthu akudutsamo Kudzera mwa Mzimu Woyera. Pamene nthawi zina, iye amafunsa anthu zimene akufuna komanso nthawi imene akhala akusautsika.

Kucheza naye munthu kumathandiza kuti mukhale ndi zithu zodziwika zimene mukhoza kupemphelera. Komanso izi zimathandiza kuti mudziwe ngati munthu akufunika uphungu wapadera atatha kupempheleredwa. Yesu nthawi zina amatha kufunsa anthu mafunso okhudza chikhulupiriro chao. Ndipo ngati panali kusakhulupirira kwina kulikonsse, iye amayamba wathana ndi kusakhulupirirako kaye asanawatumikire anthu oterewa. Werengani zitsanzo zili munsizi:

-Marko 5:1-20: Mafunso a Yesu kwa mzibambo ogwida ndi dziwanda.

-Marko 8:22-26: Afunsa munthu osapenya.

-Marko 9:14-27: Nyamata ogwidwa ndi mzimu oipa.

-Marko 10:46-52: Batumeyo wakhungu afunsidwa.

Muyenera kumufunsa munthuyo vuto. Kupempha pemphero ndi chinthu chofunika kwambiri. Yesu anamasula anthu ambiri amene anabwera kwa iye ndi kupempha zosowa zao. Kungopempha kokhako ndi chizindikiro chachikhulupiriro chimene chikhoza kubweretsa machiritso. (Yakobo 5:14-15). Muyenera kufunsa mwachindunji vuto la munthuyo. Simukuyenera kufunsa mbiri ya moyo ya munthuyo ayi.

Simukuyenera kuunikira nyengo ya munthuyo ngati phungu chifukwa inuyo udindo wanu sikupereka uphungu. Koma pali nyengo zina zimene muyenera kukhala ndi phungu kuti agwire ntchito yake ngati phungu.

Muyenera kufunsa munthu amene mukuphelerayo ngati akukhulupirira kuti Yesu akhoza kumumasura. Ndipo ngati iwo akukhulupirira, funsaninso munthuyo ngati akukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchita nthawi yomweyo. Ngati mayankho amafunso onsewa ndi ayi, munthuyo ayenera kuphunzitsidwa mau a Mulungu.

Pamene mukutumikira gulu la anthu, zikhoza kukhala zovuta kuti muthe kuyankhula ndi munthu wina aliyense payekhapayekha. Koma Mulungu ankhoza kukuonetserani nyengo za anthu ena amene ali mu gulu la anthu. Mulungu akhonsa kukutsogolerani kuti mupemphelere mwapadera athu ena.

Ngati mukuchita utumiki wa mamasulidwe ku gulu la anthu, ndikoyenera kuti muphunzitse anthu ena kuti athe kutumikira nanu. Sikoyenera kuti muchite nokha utumiki. Yesu Khristu analonjeza kuti zizindikiro zidzawatsata iwo amene akhulupirira. Izi zikutanthauza ntchito ya utumiki ndi yampingo onse osati okhulupirira mmodzi kapena kuti iwo amene ndi alaliki.

5. Muyenera kuzindikira vuto lenileni

Gwiritsani ntchito zimene mwapeza kudzera mukucheza kwanu ndi anthu amene akufuna kumasulidwa kapena chidziwitso chimene Mulungu akukuonetserani kuti muthe kuzindikira vuto lenileni.

Gawo lauzimu: Ngati mwapeza mavuto auzimu amene akuonetsera kuti pali uchimo. Muyenera kupemphelera chipulumutso, kulapa ndi chikhulukiro cha machimo.

Gawo lakuthupi: Izi zimakhudza matenda oyamba chifukw cha mphamvu yaziwanda zamatenda.

Gawo lakaganizidwe kwa munthu: Izi zimakhudza mavuto ngati mkhawa, mantha, kuwawida mtima, kulephera, kudzikonda, kusakhulukira zinthu zimene zinachitika kale.

Zinthu zimene zatchulidwa pamwambazi zimatchedwa “machiritso amkati.” Koma nthawi zambiri anthu akhala akulakwitsa pa nkhani ya Machilitso amkati. Mwachitsanzo, simukuyenera kutenga masabata ambirimбири kapena miyezi imene kuti munthu amene mukumuthandiza uja achire. Mukatero mumakhala ngati mukufuna kuchiza munthu wakale uja. Koma choyenera kutchita ndi kumuthandiza munthu uja kuti akhale cholengedwa chatsopano mwakhristu Yesu.

Cholepheleretsa chachikulu pa nkhani ya machilitso amaganizidwe a munthu ndi chikhulukiro. Payenera kukhala kuchiza maubale owonongeka. Izi zili chomwechi chifukwa pamene maganizidwe a munthu asokonekera chifukwa cha mphavu ya ziwanda, ngakhale maubale a munthuyo ndi anthu ena amasokonekera.

Mulungu watiyana kuti tikhale atumiki oyanjanitsa anthu (II Akorinto 5:18-21). Kuyanjanitsidwa kukhoza kukhala pakati pa munthu ndi Mulungu.

Muyenera kumuphunzitsa munthuyo za chikhulukiro. koma pamene muchita zinthu izi, muyenera kudziwa kuti chikhulukiro si:

- Kufuna kupeza chifukwa choti munthu sanalakwe pamene munthuyo ndi olakwitsa (mwina kumanena kuti munthuyi zinangomuvuta)
- Kukana kuti mtchitidwe wake unakhudza anthu.
- Kungovomereza kuti zithe zimene munachitazo kuti nkhani ingothona.
- Kudikira nthawi kuti muyanjanitsidwe ndi anthu amene anakhudzidwa.

Chikhulukiro chenicheni chimabwera pamene mwapanga zinthu izi:

- Kuzindikira kuti zimene munachita zinali zinthu zolakwika ndipo kuti ndi zokuonetserani zimene anthu ochimwa amapanga pa dziko.
- Kuvomereza mkwiyo wanu pamaso pa Mulungu ndi kumupempha kuti achotse kaganizidwe konse kolakwikwa. Sizikutanthauza kuti muyiwara zinthu zimene zinachitikazo ayi. Koma chimene muyenera kuchita ndi kupempha Mulungu kuti achize maganizo anu olakwika.

- Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kuti muthe kukhulukira anthu amene anakulakwirani komanso muyenera kuwakhulukira ngati mmene Khristu anakukhulukirani.

Muyenera kuzindikira kuti Mulungu amakhululuka pamene tikhulukira anthu ena. “mutikhulukire ife pamene tikhulukira amangawa athu.” Koma nthawi zina munthu amafunikanso kudzikhulukira yekha. Chifukwa zimatheka munthu kumadzimva kulakwa. Zikakhala choncho pamafunika pemphero loti munthu alandire machiritso amaganizidwe ake.

- Pali kufunika kovomereza ntchimo limene likupangitsa kuti mudzimva kuti ndinu olakwa. Muyenera kuvomereza ntchimolo ndi kupempha Mulungu akukhulukireni.
- Zindikirani kuti pamene Mulungu wakhululuka tchimo, Iye amayiwara.
- Nenerani mau opezeka pa 1 Yohane 1:8-9 ndi Aroma 8:1 kuti akugwira ntchito pamoyo wanu.
- Mwachifuniro chanu, zimasureni nokha pakudziweruza nokha. Tengani ulamuliro wa maganizo anu pakuthana ndi maganizidwe ena alionse olakwikwa.

Pamene mukutumikira, muyenera kutumikira munthu yense chifukwa vuto limene munthu angakumane nalo gawo limodzo lamoyo wake, limakhudza magawo onse amayo wa munthu. Moyo, thupi ndi mzimu ziyenera kulandira machiritso.

6. Zindikirani ngati ili nthawi yoti mutha kupemphera:

Muyenera kupanga chiganizo cha nthawi imene muyenera kupemphera pemphero lamachiritso. Nthawi zambiri, pamakhala pemphero kuti munthu amasuluridwe, koma simukuyenera kukhala odabwa pamene Mulungu akuonetserani kuti musapemphere kapena kuti mudikire kaye musanaphere.

Mu nyengo zina, Yesu amachedwetsa machiritso. Chitsanzo tikuchipeza pa nkhani ya Lazaro. Iye sanachite zambiri ku Nazareti chifukwa chakusakhulupirira kwa anthu. Mulungu akhoza kukuzani kuti muyime kaye kufikira nthawi ina. Mwachitsanzo, pokhoza kukhala kufunika kuti munthu alape machimo ake kapena kuti alandire chiphunzitso chokhudza mamasuridwe ndi zina zambiri.

7. Pemperani pemphero la mamasuridwe:

Pempherani pemphero la mamasuridwe limene liyenera kulunjika pa vuto la ziwanda limene mwapezalo. Simukuyenera kumkamiza Mulungu kuti mamasuridwe achitike chifukwa champhero lanu. Chipulumutso chimatengera chikhulupiro, chomwechonso kuti munthu amasuridwe zimatengera chikhulupiro.

Ngakhale kuti nthawi zina mphamvu ya Mulungu imabwera mwapadera kudzera mukudzodza kuti munthu amasuridwe, koma inu mukhoza kupempherabe posatengera kuti mwalandira kudzodza kwapadera (Luka 5:17) Izi zili chomwechi chifukwa Yesu anatilamura kutero kuchotsa ziwanda ngati mmene anatilamulira kuti tifalitse uthenga wabwino.

Gwiritsani ntchito anthu ena kuti akuthandizeni kutumikira ngati mukutumikira ku gulu la anthu. Pali kuchulukitsidwa kwa mphamvu pamene anthu ambiri akupemphera limodzi (Mateyu 18:19). Kutumikira limodzi ngati gulu kumathandiza kuti anthu asalamekeze munthu. Choyambilira chimene Yesu anaphunzitsa ndi chakuti muyenera kumanga mndaniyo, mukatero ndi pamene mukhoza kugwiritsa ntchito ulamuliro pa iye.

Kapena akhoza bwanji munthu kulowa m'banja la munthu wolimba, ndi kufunkha akatundu ace, ngati iye sayamba kumanga munthu wolimbayo? ndipo pamenepo adzafunkha za m'banja lace. (Mateyu 12:29)

Ngati mphavu zaziwanda zamanga munthu kudzera mu mzimu wamatenda kapena kudwaladwala, pempherani kuti munthuyo amasulidwe kunsinga zimenezi. Mwachitsanzo, Yesu anamasula mzimayi mu Sunagogi amene anali omangidwa ndi mzimu odwaladwala. Mayi ameneyu sikuti anali ndi ziwanda, koma iye amangofukika kuti amasulidwe.

Koma ngati munthu wagwidwa ndi ziwanda, muli ndi ulamuliro ochotsa ziwandazo mu dzina la Yesu Khristu. Izi sizikutengera mphamvu yanu kapena ulamuliro wanu koma dzina la Yesu Khristu. Ndi zofunika kuti mugwiritse dzina la Yesu pamene mukuchotsa ziwanda.

Chikhulupiriro, mapephero ndi kusala kudya ndi zofunika kwambiri pamene mukuchotsa ziwanda. (werengani Mateyu 17:14-21). Ichi ndi chifukwa chake zimakhala zofunika kuti mukonzekere kaye m' magawo amene atchulidwawa. Zina mwa dzida zimene Mulungu wapereka pa masulidwe ndi Mau a Mulungu (Aefeso5:17; Ahebri 4:12); mwazi wa Yesu (Chivumbulutso 12:11), ndi kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera (Machitidwe 1:8; 2:38).

Kukuwa ndi kufuula pa ziwanda sikumathandiza chinachilichoonse. Koma ndi ulamuliro umene muli nao mwa Khristu Yesu umene umapangitsa kuti ziwanda zituluke osati mmene mau anu akutulukira.

Nthawi zonse muyenera kuletsa ziwandadzo kuti zisalowenso mwa munthuyo. Ili ndi gawo lofunika kwambiri la pemphero lamamasuridwe.

Ndipo pamene Yesu anaona kuti khamu la anthu lirikuthamangira pamodzi, anadzudzula mzimu woipawo, nanena ndi uwo, Mzimu wosalankhula ndi wogontha iwe, Ine ndikulamula iwe, turuka mwa iye, ndipo usalowenso mwa iye. (Marko 9:25)

Simukueyenera kutaya nthawi yanu kuyamba kukambirana ndi ziwanda ngati zingayambe kudziointsera polankhula mau. Muyenera kuzindikira kuti kulankhula ndi lziwanda ndi koopsya kwambiri chifukwa pali mizimu yabodza. Yesu anauza ziwanda kuti dzikhale chete (Luka 4:34-35).

Mzimu Woyera adzakuthandizani pempero lamamasulidwe limene mungapemphere. Koma ngati mwangoyamba kumene utumiki umeneu, mukhoza kugwiritsa ntchito pemphero ili:

“ mudzina la Yesu Khristu ndi ulamuliro wamphamvu Yake, mau Ake, mwazi Wake ndi Mzimu Woyera ”

... izi zimakhazikitsa mphamvu ya mamasuridwe...

“...dikukumanga...”

Yesu Khristu anatilamura kuti tiyenera kumanga wamphamvuyo tisinayambe kumtulutsa”

“Ndikukulamura”

..... pemphero la mamasuliridwe ndi pemphero la ulamuliro. Mukhoza kulankula mwachete koma mutatenga ulamuliro pa mpamvu zoipa mu dzina la Yesu Khristu. Mukuyenera kuti mudzimuyang’ana m’maso munthuyo pamene mukuyankhula.

“Mzimu wa _____ kapena iwe mzimu onyansa wa satana”

... ngati mwatha kuzindikira mzimu kudzera mu muchidziwitso chazimu kapena chakuthupi, muyenera kutchula mzimuwo kapena ngati simukudziwa kanthu, ingotchulani kuti mzimu onyansa”

“Samuka....”

“Ili ngi gawo lochotsa kapena kuthamangitsa ziwanda”

“mosabweleretsa chisokonezo_____tchulani dzina la muthu amene akumasuridwayo kapena mukhoza kutchura mau oti wina aliyense ali muno”

... nthawi zina chiwandacho chimayesa kufuna kuvulaza munthuyo.

“ndikukaniza kulowanso mwa munthu ameneyu....”

... kumbukirani kuti Yesu amagwiritsa ntchito mau amenewa.

“ndikumasula Mzimu Woyera kuti adzadze munthu ameneyu ndi mphamvu yamamasulidwe a Yesu Khristu”

.... Tiyenera kumanga komanso kumasula. Ngati mwazindikira kuti pali mzimu wapadera umene ukugwira ntchito, muyenera kumasula mzimu wina otsutana ndi mzimu umene mwapezao. Mwachitsanzo, muyenera kumanga mzimu odzikuzza ndi kumasula mzimu odzichepetsa.

Simukuyenera kuchita chionetsero cha utumiki umeneu ndi cholinga chokopa chikhamu cha anthu. Yesu ataona kuti zimene chiwanda chimachita zimakopa khamu la anthu, iye analamura chiwandacho kuti chituluke.

Ndipo pamene Yesu anaona kuti khamu la anthu lirikuthamangira pamodzi, anadzudza mzimu woipawo, nanena ndi uwo, Mzimu wosalankhula ndi wogontha iwe, Ine ndikulamula iwe, turuka mwa iye, ndipo usalowenso mwa iye. (Marko 9:25

Simukuyenera kuchotsa ziwanda kuti zipite ku gahena chufukwa Yesu ndi ophunzira ake sanachitepo zimenezi. Ulamuliro umene tili nao ndi omanga, ochotsa ndi kumasula kokha basi. Pali nthawi yokhazikitsidwa imene dziwanda zidzaweruzidwa mtsogolo. Dziwanda zinalankhula ndi Yesu nati:

... Ndipo onani, anapfuula nati, Tiri nanu ciani, inu Mwana wa Mulungu? mwadza kuno kodi kutizunza ife, nthawi yace siinafike? (Mateyu 8:29)

Pemphero pa anthu amene akudzidwa ndi ziwanda likhoza kuperekedwa posanjika manja kapena ayi. Pa Luka 13:11-13, Yesu Khristu anasanjika manja mzimayi ozunzidwa ndi mzimu wamatenda. Koma nthawi zina Iye samasanjika manja, iye amangolankula kuchiwandacho.

8. Muyenera kulemekeza Mulungu chifukwa cha mayankho ake:

Pamene mwamaliza kupephera, muyenera kutamanda Mulungu chifukwa cha mamasulidwe. Kumbukirani nkhani ya akhate khumi aja. Onse anachiritsidwa koma ndi mmodzi yekha amene anabwelera kudzathokoza ndipo iye yekha ndi amene anachiritsidwa kwa thunthu. Muyenera kukhulupirira zimene analonjeza kuti adzachita. Ndipo mukuyenera kumuthokoza.

KUZINDIKIRA ZA MAMASULIDWE.

Nthawi zina pamene munthu wagwidwa ndi ziwanda, ziwandazo zimatuluka ndi mphamvu, mwachitsanzo munthu amatha kumangolira kapena kudziponya pansu. Koma pamane chiwanda chatuluka, munthu amamva kumasulidwa, chimwemwe ndi kupepukidwa ngati watulidwa chinthu cholemera.

KUYENDERANSO ANTHU OMASURIDWA:

Pamene mamasulidwe achitika, anthu amene ali ogwidwa ndi ziwanda ayenera kuthandizidwa ndi pemphero kuti alape, ndikusiyana zonse zakale zimene zinali zolumikizana ndi ntchito za Satana. Ngati munthuyo anali ndi zinthu za nyanga monga zithumwa, mafano ndi zinthu zina zaufiti. Zinthu zimenezi ziyenera kuonongedwa.

Ndi zofunika kwambiri kuti anthu amene amasulidwa ayenderedwebe. Pamene chiwanda chachotsedwa, chimafunafuna thupi lina loti chilowemo. Pamakhala chiopsezo choti chiwanda kapena ziwanda zimatha kubweleranso mthupi la munthu koma ngati ziwanda zabweleranso mwa munthu, zimabwera ndi mphamvu. Izi zikugwirizana ndi chiphunzitsa cha Yesu kuti pamene chiwanda chachoka mwamunthu, chimasiya malo opanada kanthu.

Pamene paliponse mzimu wonyansa ukaturuka mwa munthu, upyola malo opanda madzi nufunafuna mpumulo; ndipo posaupeza unena, Ndidzabwera kunyumba kwanga kumene ndinaturukako; ndipo pofika, uipeza yosesa ndi yokonzeka. Pomwepo, upita nutenga mizimu yina isanu ndi iwiri yoipa yoposa ndi uwu mwini; ndipo ilowa nikhalira komweko; ndipo makhalidwe otsiriza a munthu uyu aipa koposa oyambawo. (Luka 11:24-26)

Pamene chiwanda chatuluka mnthupi la munthu, chimakhala chosowa mtendera komanso chosakhazikika kunja kwa thupi la munthu. Chiwanda chimakwanitsa zolinga za Satana pokhapokha ngati chili mnthupi la munthu. Ichi ndi chifukwa chake kungochotsa chiwanda chokha sikokwanira ayi. “Nyumba yauzimu” Iyenera kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera komanso iyenera kubadwa mwatsopano. Chifukwa cha ichi, ndikofunika kuwayendera anthu amene amasuridwa. Munthu amene wamasuridwa ayenera kudzadzidwa ndi Mau a Mulungu komanso ayenera kuchita chiyanjano ndi anthu ena okhulupirira.

Anthu amene amasuridwa ku mphamvu ya ziwanda ayenera kulimbikitsidwa kuti achitire umboni wao kwa anthu ena. Yesu anauza munthu ogwidwa ndi ziwanda ku Gadara kuti:

Ndipo posapeza polowa naye, cifukwa ca unyinji wa anthu, anakwera pamwamba pa chindwi, namtsitsira iye poboola pa chindwi ndi kama wace, namfikitsa pakati pomwe pamaso pa Yesu. Ndipo iye, pakuona cikhulupiriro cao, anati, Munthu iwe, macimo ako akhululukidwa. (Marko 5:19-20)

CHITETEZO KU MPHAMZU YA DZIWANDA

Pali njira zambiri zimene mukhoza kutsata kuti mudzitetze ku mphamvu ya ziwanda. Njira yothandiza kwambiri yodzitetze ku ziwanda ndi kulandira Yesu ngati mphulumutsi chifukwa ziwanda zizimakhala mwa munthu obadwa mwatsopano. Muyenera kupewa tchimo chifukwa ndi tchimo limene limapereka mwayi kwa Satana. Mumapereka mwayi kwa Satana kuti athe kukugwiritsani ntchito.

Muyenera kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera chifukwa mzimu wa Mulungu ndi mizimu yoipa sizikhalira limodzi.

Simukuyenera kukhala ndi chidwi chachikulu ndi ziwanda. Sizolakwika kuphunzira zimene mau a Mulungu amakamba zokhudzana ndi ziwanda. Simukuyenera kuwerenga mabuku achikunja okhudza ziwanda, kapena kuphunzira nao maphunziro achikunja okhudza ziwanda ndi cholinga choti mudziwe zambiri. Simukuyeneranso kuchita zinthu izi: kupita kwa asing'anga, amaula kapena anthu owombeza ndi ena amatsenga. Simukuyenera kutumikira Mulungu yamafano. kapena kulora kuti mafano apezeke panyumba panu.

Mafano osema a milungu yao muwateothe ndi moto; musamasirira siliva ndi golidi ziri pa iwo, kapena kudzitengera izi; mungakodwe nazo; pakuti izi zinyansira Yehova Mulungu wanu. Musamalowa naco conyansaci m'nyumba mwanu, kuti mungaonongeke konse pamodzi naco; muziipidwa naco konse, ndi kunyansidwa naco konse; popeza ndi cinthu coyenera kuonongeka konse. (Deuteronomo 7:25-26)

Ndi zinthu zofunika kwambiri kuti musamalitse masankidwe a anthu amene mumacheza nao, zimene mumayankhula. Ndi zofunikanso kukhala ndi ulamuliro ku nkhani zakuthupi.

Muyeneranso kumenye nkondo yolimbana ndi yofuna kudzitetze ku mphamvu ya ziwanda

KUYENDERA PERETE

1. Lembani vesi yotsolera kuchokera kuzolembedwa zankhondo

2. Tchulani mitundu itatu imene imalimbana ndi thupi, mzimu, ndi moyo wa munthu?

3. Kodi mphatso ya chidziwitso ndi yofunika bwanji polimbana ndi mphamvu zakumidima?

4. Kodi kugwida ndi chiwanda ndi chiani?

5. Kodi ndi chikhalidwe chiti chimene munthu ogwidwa ndi ziwanda amaonetsera.

6. Kodi kukhala ndi chidwi chachikulu ndi chiani?

7. Kodi ndi chikhalidwe chiti chimene munthu amene ali ndi chidwe chachikulu ndi ziwanda amaonetsera?

8. Kodi kuzunzidwa ndi ziwanda ndi chiani?

9. Tchulani makhalidwe amene munthu ozunzidwa ndi dziwanda amaonetsera

10. Fototozerani mwachidule ndondomeko za Baibulo zothana ndi mphamvu ya ziwanda.

(Mayanko amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

MACHITACHITA ALUSO

Werengani zitsanzo zili munsimu zimene zikuonetsera mmene Yesu anachitira ndi mphamvu ya ziwanda.

Nkhani: Mzimayi wa mzimu odwaladwala mu Sunagogi. (Luka 13:10-17)

Kufotokozero mwachidule: Mzimayiyu anapita kukapemphera ku Sunagogi patsiku la la sabata. Yesu anaitana iye nati: “mwana mwamkazi wa Abrahamu” Izi zikuonetsera kuti Iye anali olungama ndi oyera mtina. Komabe iye anakhala chidwalire kwa dzaka makumi asanu ndi zitatu ali chidwalire.

Mu utumiki wa Yesu Khristu, Iye amasiyanitsa pakati pa matenda achilengedwe amene amatha kuchizidwa ndi kusanjika manja kapena kudzodza mafuta, ndi matenda amene amabwera chifukwa cha mphamvu yaziwanda. Zikakhala kuti munthuyo ndi okhulupirira koma wamangidwa kunja ndi mphamvu yaziwanda, munthu omangidwayo amamasuridwa. Koma ngati chiwanda cha kudwaladwa chagwira munthu amene siokhulupirira, chiwandacho chimathamangitsidwa.

Chifukwa chakuti mzimayi uja anamasuridwa nthawi yachipembedzo, izi zinabweretsa mpungwepungwe pakati pa atsogoleri achipembedzo amene anatsutsana nazo zimenezi. Nthawi zambiri pamene pali kulimbana ndi mizimu yoipa pamakhala otsogoleri amene ametsutsa zimenezi. Ena mwa atsogoleri amakanan kuti ziwanda zili ndi mphamvu yotha kumanga kapena kusautsa munthu.

Yesu anasanjika manja ake pa mzimayi uja musunagogi, ndipo iye anamasuridwa. Pamene anachiritsidwa, Iye anaremekeza Mulungu. Pamene munthu wamasuridwa, ulemelero onse uyenera kupita kwa Mulungu osati kwa munthu amene Mulungu wamugwiritsa ntchito pobweretsa mamasuridwe.

Nkhani: Kabuthu ka Mkazi waku Suro –Fonika (Marko 7:24: -30: Mateyu 15:21-28)

Kufotokozero mwachidule: kabuthu kanamangidwa ndi mzimu onyansa umene mai ake anauzindikira chifukwa cha zimene mziwo umaonetsera kunjja. Iye anafotokoza kuti mwana wake wagwidwa koopsya ndi chiwanda. Yesu anachiritsa mtsikanayu chifukwa cha chikhulupiriro chachikulu chimene anaonetsera mayi wake. Mtsikanayu sanabwere naye pamaso pa Yesu. Izi zikuonetsera kuti utumiki wa mamasuridwe kuti uchitike, sizikutengera kuti munthuyo akhale pomwepo. Chitsanzo chimenechi chikuonetsera kuti ngakhale ana nao akhoza kugwidwa komanso kusautsika ndi ziwanda.

Nkhani: Mwana ogwidwa ndi mzimu osalankhula ((Marko 9:14-29; Mateyu 17:14-21; Luka 9:37-43).

Tate amwama ameneyu anufunafuna Yesu ndi cholinga choti achiritse mwake wake. Chifukwa chongwidwa ndi mzimu oipa, mwanayu samamva ndi kuyankhula kumene. Malinga ndi mmene Marko, Luka ndi Mateyu alembera nkhani imeneyi, zikuonetsa kuti mnyamatayu amasautsika ndi chiwandachi. Iye amatha kudziponya pamoto kapena mmadzi. Nthawi zina mnyamatayu amakomako, kuchita thovu kukamwa komanso ndi kukukuta mano. Nthawi zambiri amavulara chifukwa chachiwandachi, ndipo chimamupangitsa kuti achepe thupi kapena kuti kuonda. Ophunzira a Yesu anayesa kuti achotse chiwanda chimenechi koma anakanika.

Luka akufotokoza kuti pemene mnyamatayu anafika pamaso pa yesu, chiwanda chinampangitsa kuti akomoke. Koma Yesu anadzudzura chiwandachi ndipo mnyamatayu anamasuridwa. Luka akufotokoza kuti Yesu anafunsa atate amwanuyu kutalika kwa nyengo ya vuto la mwana wao. Tate a mwanayo anati mwana wao anali ndi vutoli chiyambireni umwana wake.

Yesu anatsindika kwambiri zachikhulupiriro kwa bambo amwanayu, kenako Iye analamura mzimu wakusayankhula ndi kusamva kuti utuluke ndi kuulamuranso kuti usabwelerenso. Mnyamatayu anafuula kwambira moti anthu ena amaona ngati wamwalira. Koma Yesu anagwira mkono wake ndikumudzutsa.

Ophunzira a Yesu atafunsa chifukwa chimene analephelera kuchotsa chiwanda mwa mwana uja, Iye anawayankha nati:

Ndipo Iye ananena kwa iwo, Cifukwa cikhulupiriro canu ncacing'ono: pakuti indetu ndinena kwa inu, Mukakhala naco cikhulupiriro monga kambeu kampiru, mudzati ndi phiri ili, Senderapo umuke kuja; ndipo lidzasendera; ndipo palibe kanthu kadzakulakani kosacitika. (Mateyu 17:20)

Zimene Yesu anawayankha zinaonetsera kufunika kwa pemphero, chikhulupiriro ndi kusala kudya ngati njira yothana ndi ziwanda. Zinaotseranso kuti ziwanda zina ndi zovuta kutuluka kusiyana ndi zina. Chifukwa cha ichi, Yesu anafotokoza kuti zina zimatheka ndi pemphero ndi kusala kudya.

Nkhani: wachiwanda mu sunagogi: (Marko 1:23-28; Luka 4:31-37).

Kufotokoza mwachidule: Ngakhale kuti munthu ameneyu anali mu sunagogi, Yesu sakumutichula Iye kuti ndi mwana wa Abrahamu kapena kuonetsera kuti iye anali munthu okhulupirira Mulungu. Ndi zotheka kuti mumpingo mukhoza kupezeka anthu osakhulupirira komanso ogwidwa ndi ziwanda. Kukhala gawo limodzi la tchalitchi kapena mpingo sizimathanthauza kuti ndiye kuti munthu sangakhudzidwe ndi ziwanda kapena kuti munthu ndi obadwa mwatsopano. Malinga ndi nkhanayi, zikuoneka kuti mwamunthuyi munali ziwanda zingapo. Izi zikuoneka chifukwa chakuti iye anagwiritsa ntchito mau oti “ife.” Pamene chiwanda chinayamba kuyankula, iye anachilamula kuti chikhale chete. Anthu amene anaona izi zikuchitika anazizwa ndi ulamuliro umene Yesu anali nao pothanan ndi mzimu onyansa.

Nkhani: wakhungu, osalankhula ndi waziwanda (Mateyu 12:22-29; Marko 3:22-27; Luka 11:14-22).

Kufotokoza mwachidule: Kusaona ndi kusayankhula linali gawo limodzi logwidwa ndi ziwanda. Yesu anachiza munthuyi poturutsa chiwanda chimene chinali mwa munthuyu. Iye anayamba kuona ndi kulankhula. Kudzera mukumasuridwa kwa munthu ameneyu, Yesu Khristu anapereka chiphunzitso chachikulu chokhudza kuchotsa ziwanda. Mwachidule zina mwa zinthu zimene Iye anaphunzitsa ndi izi:

- Nyumba imene ndi yogawikana singaimen pa ziwanda. Thupi limene ziwanda zimakhalamo ndiye nyumba ya ziwandazo. Chifukwa cha ichi, ndi zosatheka kuti Mzimu wa Mulungu ndi ziwanda kukhalira nyumba imodzi.
- Mafumu kapena mizinda yogawikana singaime.
- Kuchotsa ziwanda ndi gawo limodzi la utumiki wa Ufumu wa Mulungu.
- Ndi zofunika kumanga Satana musanamutulutse (musanatulutse ntchito zake)
- Wina aliyense ali pa nkondo. Ngati simuli mbali ya Yesu, ndiye kuti ndinu otsutsana naye.
- Pamene chiwanda chachoka mwamunthu, chimafunafuna kuti chilowenso mwa munthu.
- Ngati munthu amene wamasuridwa saika kanthu nyumba yake yauzimu, chiwanda chija chimabwelera ndi ziwanda zina. Ngati munthuyo anali wabwinoko pachiyambi, iye amakhala oipitsitsa.

Nkhani: wachiwanda waku Gerasa (Marko 5:1-20; Mateyu 8:28-34; Luka8:26-34)

Kufotokoza mwachidule: Malinga ndi Mateyu, anthu awiri ogwidwa ndi ziwanda, anali amphamvu kwambiri kotere kuti panalibe muthu amene akanatha kuwagwira. Ndipo azimbambowa anali kukhala kumanda. Luka akufotokoza mamasuridwe a mzimbambo mmodzi amene mamasuridwe ake anali akulu mu utumiki wa Yesu Khristu.

Azimbambowa anali ndi ziwanda zambiri ndi aukali. Chifukwa cha ichi, zinali zovuta kuti athe kukhala ndi anthu ena Kumudzi. Ziwanda mwa munthu m’modzi zimafotokoza kuti izo ndi “chikhamu” chifukwa chakuti zinalipo zambiri. Kunali kovuta kuti mnyamatayo akanatha

kumangidwa chifukwa chakwauli wake. Ziwanda zimamusautsa kwambiri kotere kuti amafika podzicheka ndi miyala komanso iye samavala chinachilichonse.

Ziwanda zinamuzindikira Yesu ndipo zinafunsa ngati Iye cholinga chake chinali kuzichotsa nthawi isanafike. Nthawi imene imatchulidwa apayi ikutanthauza nthawi yachiweruzo chakugahena. Ziwandazo zinapepha kuti zisachotsedwe. Izi zikuonetse kuti ziwanda zimatha kutumizidwa ndi Satana kuti zikagwire ntchito ku dera limene Satanayo akufuna. Yesu analora ziwandazo kuti zilowe munkhumba ndipo ngati zotsatira, nkumbazo zinafa. Anthu amudzi anapempha kuti Yesu awachokera mmudziwa mwao. Kwa anthu amenewa, khumba zao zinali zofunika kuposa mamasuridwe ku mphamvu ya ziwanda.

Nkhani zina: kupatula nkhani zimene zakambidwazi, Baibulo limafotokoza utumiki wa Yesu kwa anthu amene anakhudgidwa ndi mphamvu ya ziwanda.

- Mu ndime izi Mateyu 4:24; Luka 6:18., mau akuti kuchiritsa akugwiritsidwa ntchito pofuna kuonetsera mmene Yesu anachitira ndi anthu ogwida ndi mizumu ya ziwanda.
- Mu ndime izi Marko 1:32- 34,39; 6:13, Mau oti kutulutsa akugwiritsidwa ntchito Pofuna kuonetsera njira imene Yesu amagwiritsa ntchito.
- Pa Luka 4:41 akufotokoza kuti ziwandanda zinatuluk. Pamene Luka 7:21 akufotokoza kuti anawachiritsa. Mateyu 8:6 akufotokoza kuti anaziturutsa ndi mau ake
- Pa Marko 16:9 and Luke 8:2-3 amafotokoza kuti Yesu anaturutsa ziwanda zingapo mwa Mariya waku Magadara

2. Nthawi zina Mulungu amagwiritsa ntchito ziwanda ndi cholinga chofuna kukwaniritsa zolinga zake. Werengani I Samueli 16:14 ndi II Akorinto 12:7. Ahabu analangidwa ndi mzimu onyenga chifukwa cha machimo ake. Mulungu Anaika mzimu onyenga mwa aneneri ake kuti asocheretse iye. Werengani I Mafumu 22:23. Chimodzimidzi, ziwanda zinaitanira ankhondo a Amagedoni kuti awonongeke. (werengani Chivumbulutso 16:13-16)

3. Mphamvu ya ziwanda imatha kukhala ndi ulamuliro pa maiko komanso pa amayi ndi abambo. Werengani chitsanzo chopezeka pa Danieli 10 pamene akuonetsa za Karonga waku Peresia. Zimaoneka kuti karonga ameneyu anali ndi ulamuliro pa zochitika za kudera limeneli. Buku la Chivumbulutso limafotokoza ntchito ya ziwanda pa maiko. Werengani Chivumbulutso 16:13-16.

4. kucheza nthabwala zokhudza ziwanda si zinthu zoyenera. Werengani II Petro 2:10-11. Paife tokha tilibe mphamvu zodzudzura ziwanda kapena Satana.

5. Yesu anapereka ulamuliro ochotsa ziwanda kwa ophunzira ake. Werengani ndime izi zimene zikuonetsera mmene ophunzira anagwiritsira ntchito mphamvu imene anapatsidwa Marko 9:38; Luka 10:17; Machitidwe 5:16; 8:7; 16:16-18; 19:11-12.

6. Werengani ma vesi awa amene akugwiritsa mau oti “ogwidwa:” Mateyu 4:24;

8:16,28,33; 9:32; 12:22; Marko 1:32; 5:15-18; Luka 8:36; Machitidwe 8:7; 16:16.

7. Yesu anazunzidwa ngakhale analibe tchimo. Yesaya 53:7. Pamene Hezekiya anasautsidwa, Iye anapempha Mulungu kuti amulanditse. Yesu anachiritsa onse osautsika ndi Satana: Machitidwe 10:38.

Werengani zoonjezera zina zokhudza kusautsika:

- Ndi anthu oipa: Salimo: 17:9
- Ndi adani athu Salimo 106:42
- Ndi anthu odzikuza: Salimo119:122
- Ndi achuma: Yakobo 2:6

CHAPUTALA 22

OKHUDZIDWA NDI NKHONDO

ZOLINGA

Pamapeto paphunziro ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza chiyamb cha mazuzo pa dziko lapansi.
- Kufotokoza mmene mazuzo amayambira pa moyo wa okhulupirira.
- Kuonetsera kumvetsa maonedwe oyenera a chizuzo.
- Kufotokozerera kufunika kwa chizuzo.
- Kufotokozerera kusiyana kwa kudutsa mu mafunde chifukwa cha chifuniro cha Mulungu ndi kudutsa m' mafunde chifukwa chosemphana ndi chifuniro cha Mulungu.

VESI YOTSOGOLER KUCHOKERA MUZEMBA ZA MKONDO:

Umve zowawa pamodzi nane monga msilikari wabwino wa Kristu Yesu. (2 Timoteo 2:3)

MAU OYAMBA

Nkhondo ina iliyonse yakuthupi imakhala ndi anthu amene amavulala nayo kapena kuphedwa kumene. Ena akavulala amachira ndi kubweranso kukamenya nkhondo pamene ena samachira. Izi ndi chimodzimodzi ndi nkhondo yauzimu imene timakhala tikumenya. Ankhondo a chikhristu amakhudzidwa ndi nkhondo za Satana, naonso amakhudzidwa ndi zotsatira za chizuzo

Ambiri mwa ife sitimakonda kumva cha chizuzo. Nthawi zambiri sitimamva mauthenga okhudza mazuzo. Anthu timafuna kumva mauthenga okhudza chigonjetso komanso kuchita bwino. Sikuti izi ndi zinthu zolakwikwa ayi chifukwa zili mbali imodzi ya mau a Mulungu. Nkhani ya mazuzo imapewedwa kukambidwa chifukwa pali zinthu zina zokhudza chizuzo zimene zili vovuta kufotokozerera kapena kuzimvetsetsa. Koma sikuti Baibulo ndi buku la malonjezano a moyo ochuluka okha ayi. Limafotokozeroso za mazuzo a anthu olungama ndi osalungama omwe.

Yesu atayamba kukamba za mazuzo amene adzakumane nao pamtanda paja, ambiri mwa anthu amene amamutsata anayamba kumuthawa. (Yohane: 6:55-66). Iwo anali ndi chiyembekezo choti Mesiya olonjezedwayo adzalamulira ndi mphamvu komanso ulemelero. Koma chifukwa chakuti Yesu amakamba za mazuzo, zimene zinali zosemphana ndi zimene amayembekezera, ambiri anamuthawa. Chimodzimodzi nanunso, ngati simungamvetse chizuzo ndi zotheka kuti mukhoza kudzasiya kutsata Yesu mutakumana ndi chizuzo. Mukhoza kukhala munthu ogonjetsedwa pa nkhondi mmalo mokhala ogonjetsa pankhondo.

Phunziro ili likhazikika pa anthu okhudzidwa ndi nkhondo, “anthu amene avulara pakumenyana.” Muphunzira mmene mungachite pemene mukumana ndi nsautso, komanso mmene mungatumikire anthu amene akukumana ndi nyengo zovuta.

GWERO MAMAZUZO

Mulungu Sanalenge mazuzo. Koma chizuzo chinalowa dziko lapansi chifukwa cha tchimo la munthu limene oyambitsa wake anali Satana(Genesis3). Chifuka chakuti munthu anagonjera chiyeso cha Satana, mazuzo analowa dziko lapansi. Kotera kuti ntchimo limene linabweretsa chizuzo, chiyambi chake ndi Satana. Koma chosangalatsa kwa anthu okhulupirira ndi chakuti, Mulungu amatha kugwiritsa chizuzo chimene Satana amafuna kutiononga nacho kuti akakwaniritse malingaliro ake abwino pa ife. Mulungu anatha kusintha munthu okhudzidwa ndi chizuzo kukhala munthu ogonjetsa.

ZIFUKWA ZOKUMANIRA NDI CHIZUZO

Baibulo limakamba zambiri zokhudza chizuzo, mavuto ndi nsautso. Pofuna kufotokoza mwachidule, pali njira zisanu zimene chizuzo chikhoza kubwera mmoyo wa munthu okhulupirira. Ndipo chizuzo chonse chimene mungakumane nacho mmoyo wanu chikhoza kubwera kudzera mu njira imodzi mwa njira zimenezi:

KUCHOKERA KWA ANTHU ENA OKUZUNGULIRANI

Mazuzo akhoza kuchokera kwa anthu amene akuzungulirani inu. Yosefe ndi chitsanzo chabwino cha izi. Ngakhale kuti panalibe chimene iye analakwitsa, iye anagulitsidwa ku ukapolo ndi abale ake, ananamiziridwa ndi mkazi wa Potifara komanso anayiwalidwa ndi anthu amene anawathandiza ali mundende.

Tsopano musaphwetekwe mtima, musadzikwiyira inu nokha, kuti munandigulitsira ine kuno, pakuti Mulungu ananditumiza ine patsogolo panu kuti ndisunge moyo. Ndipo Mulungu anatumiza ine patsogolo panu kuti ndikhazike inu mutsale m'dziko lapansi, ndi kusunga inu amoyo ndi cipulumutso cacikuru. (Genesis 45:5,7)

NYENGO ZA MOYO.

Njira yachiwiri imene mazuzo amabwera ndi kudzera nyengo zathu zamoyo wa tsikunditsiku. Chitsanzo chabwino ndi Naomi amene anakumana ndi imfa ya mamuna wake komanso ndi ana ake. Nkhaniyi ukupezeka mu buku la Rute.

Imfa ndi mbali imodzo ya moyo wathu kufikira nthawi imene Yesu Khristu adzabwerenso kachiwiri ndikugonjetsa imfa. Imfa inalowa pa dziko lapansi chifukwa cha tchimo la munthu mmodzi. Ndipo imfa ndi chinthu chachilengedwe chimene munthu wina aliyense adzakumane nacho munthawi yoikikayo (Ahebri 9:27)

UTUMIKI WANU

Chifukwa china chikumanira ndi chizuzo ndi chifukwa kumtumikira Mulungu. Chipangano Chatsopano chimakamba za kukumana ndi Mazuzo chifukwa cha dzina la Ambuye. (Machitidwe

9:16), chifukwa cha Khristu, (Afilipi 1:11-12) chifukwa chakuchita bwino (I Petro2:19-20; 3:17), chifukwa cha moyo wanu wangwiro (I Peter 3:14), chifukwa chakuti ndi inu okhulupirira (I Petro 4:15-16), ndi chifukwa chachifuniro cha Mulungu (I Petro 4:19).

Mtumwi Paulo ndi chitsanzo chabwino cha kukumana ndi mazuzo chifukwa cha utumiki. Anthu ena amaona ngati kukumana ndi mazuzo ndi chizindikiro cholephera komanso chopanda chikhulupiriro. Koma ngati izi zili chonchi, ndiye kuti Paulo mtumwi anali munthu olephera kwambiri mu mbiri yonse ya mpingo komanso opanda chikhulupiriro.

Mtumwi Paulo anafotokoza kuti anathodwa kwakulu komanso anakumana nd nsautso waukulu (1 Akorinto 1:8) Iye akupereka chithunzithunzi china chimene chimene sichikupereka lonjezano lina lilironse la mtendere komanso kuchita bwino. Pamene Mtumwi Paulo anaitanidwa ku utumiki, iye anauzindwa za mazuzo akulu amene adzakumane nao chifukwa cha khristu Yesu (Machitidwe 9:16)

Yankho la Paulo pankhani yamazuzo ndi lakuti kuti kwapatsidwa kwa inu kwaufulu cifukwa ca Kristu, si kukhulupirira kwa iye kokha, komatunso kumva zowawa cifukwa ca iye” (Afilipi 1:29)

Paulo sanali yenkha pa utumiki wake wachizunzo. Mpingo onse wachipanagano Chatsopano unakumananso ndi chizunzo. Pa Ahebri chaputala 11 pali mbiri ya chizunzo chimene okhulupirira anakumana nacho. Koma ambiri mwa amayi ndi abambo amenewa anapulumsidwa ndi mphamvu ya Mulungu. zitseko zandende zinatseguka ndipo anatuluka ngati mfulu. Iwo anagamulidwa kuti aponyendwe mung’ anjo zamoto koma, iwo anatuluka osakhudzidwa ndi moto.

Koma ena mwa amayi ndi abambo amene anali okhulupirira sanalanditsidwe kumazuzo awo. Iwo anazunzidwa, kumangidwa ngakhale kuphedwa kumene chifukwa cha umbono wa uthenga wabwino (Ahebri 11:36-40). Timatsindika za chikhulupiriro cha anthu amoyo, koma Mulungu amaonetseranso mphamvu yake pamene okhulupirira akumwalira. Ichi ndi chikhulupiriro chenicheni chimene chimaonekera ngakhale munyengo zoipa osangoti munyengo yabwino pamene chiomboro cha Mulungu chimaonekera.

MKHONDO YOCHOKERA KU ZINTCHITO ZA SATANA:

Mazunzo okhoza kulowanso mmoyo wanu chifukwa cha ntchito za Satana. Chitsanzo cha bwino ndi nkhani ya Yobu. Buku la Yobu likuyankha funso lakuti “ndi chifukwa chiani anthu olungama amakumana ndi mavuto”

Umboni ochokera kwa Mulungu unali oti Yobu anali munthu olungama (Yobu 1:2). Yobu sanakumane ndi mavuto chifukwa chakuti anachimwa ngati mmene anzake amafotokozerana. Iwo amakhulupirira kuti ngati Yobu angalape, ndiye kuti nyengo zake zisintha. Anzake a Yobu amatenga zinthu malingana ndi mmene amazionera iwo ngati chnoonadi chimene chimagwira

ntchito pa Munthu wina aliyense. Izi zili ngati kunena kuti “chifukwa chakutu Mulungu anamasula Petro mundende, chomwechonso achita izi pamoyo wanu. Koma izi sizoonza chifukwa anthu ambiri apheledwa ali kundende ngakhale kuti anali ndi chikhulupiriro chachikulu.

Tiyenera kusamalitsa ndi mmene timaonera mazuzo amene anthu ena akukumana nao chifukwa tikhoza kuwaganizira kuti akuzunzika chifukwa cha uchimo, kusakhulupirika kapena chifukwa cha kusakhulupirira. Baibulo limaphunzitsa kuti munthu ochimwa amakolera chivundi chifukwa chakufesa kuthupi (Agalatiya 6:8) Koma sitinganene kuti anthu olungama pamene akumana ndi zovuta ndiye kuti akukolera zimene anafesa.

Yobu sanakumane ndi mavuto chifukwa chakuti anachimwa ayi, iye anali munthu olungama. Ndipo anali Mulungu amene amachitira umboni wachiyero cha Yobu. Kunali kumwamba kokha kumene kumadziwa choyambitsa chenicheni cha mazuzo a Yobu. Nkhondo yauzimu inali ikuchitika mumtima mwake, mmaganizo ake angakhale mikudzipereka kwake kwa Mulungu.

Nkhondo yaikulu imakhala ikuchiti mdziko lauzimu chifukwa cha inu. Nkhondo imeneyi imaonekera mu nyengo zolimba za moyo wanu. Koma mfundo yaikulu yopezeka mu nkhani ya Yobu ndi yakuti paline chinthu chimene chingachitike pamoyo opanda Mulungu kudziwa. Mulungu samabweretsa chizunzo pamoyo wanu. Chizunzo chimachokera kwa Satana, koma malire ake amakhazikitsidwa ndi Mulungu.

MACHIMO ANU OMWE:

Njira yachisanu imene chizunzo chimalowera mmoyo wanu ndi chifukwa cha uchimo wanu omwe. Yona ndi chitsanzo chimodzi cha mazunzo amenewa. Chifukwa chakusamvera Mulungu, Yona anatenga njira Yosempana ndi kumene Mulungu anamuuza kuti akalalikire uthenga Wabwino mu mzinda wa Nenevi. Iye anakumana ndi mphepo yamphamvu panyanja imene zotsatira zake zinali kukathera m’ mimba mwasomba chifukwa chauchimo wake.

Mavuto ayenera kuonedwa ngati chenjezo kuti tiunikirensa njira zathu pamaso pa Mulungu. chifukwa mwina ngati Yona, mukhoza kukhala kuti mukukumana ndi mavuto chifukwa cha uchimo wanu. Baibulo limaonetse kuti Mulungu amalanga iwo akusamvera mau ake. Kulanga kumatathauza kupereka mwambo, kukonza kapena chidzudzulo.

Chango ciri conse, pakucitika, sicimveka cokondwetsa, komatu cowawa; koma citatha, cipereka cipatso ca mtendere, kwa iwo ozoloweretsedwa naco, ndico ca cilungamo. (Ahebri 12:11)

Mulungu amagwiritsa ntchito mazunzo pofuna kukukonzani komanso kubwenzeretani kuchifuniro chake pamoyo wanu.

Ndisanazunzidwe ndinasokera; Koma tsopano ndisamalira mau anu. Kundikomera kuti ndinazunzidwa; Kuti ndiphunzire malemba anu. Ndidziwa kuti maweruzo anu ndiwo olungama, Yehova, Ndi kuti munandizunza ine mokhulupirika. (Masalmo 119:67,71,75)

KAONEDWE KOYENERA KAMAZUNZO

Msautso sichizindikiro chakuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Baibulo limafotokoza kuti nsautso wa olungama uchuluka (Salimo 34:9) Pamene mukumana ndi masautso osati chifukwa chakuti mwachimwa, muyenera kukhala ndi kaonedwe kabwino ka mazunzo anuwo. Muyeso weniwen wauzimu wani ndi mmene mumachitira mukakumana ndi nyengo za msautso.

Ukalefuka tsiku la tsoka Mphamvu yako icepa. (Miyambi 24:10)

Baibulo likuonetsa mmene muyenera kuonera zinthu pamene mwakumana ndi msautso chifukwa cha chifuniro cha Mulungu

koma akamva zowawa ngati Mkristu asacite manyazi; koma alemekeze Mulungu m'dzina ili. (1 Petro 4:16)

Muyenera kupereka moyo wanu onse kwa Mulungu pozindikira kuti Mulungu chikozero chake ndi chabwino munyengo zonse.

Koteronso iwo akumva zowawa monga mwa cifuniro ca Mulungu aike moyo wao ndi kucita zokoma m'manja a Wolenga wokhulupirika. (1 Petro 4:19)

Muyenera kukhala okondwera pamene mukumana ndi chizunzo chifukwa chachifuniro cha Mulungu.

Paulo akufotokoza kuti:

kondwerani m'ciyembekezo, pirirani m'masautso; limbikani cilimbikire m'kupemphera, (Aroma 12:12)

ndipo tigwiritsa nchito, ndi kucita ndi manja athu a ife tokha; polalatiidwa tidalitsa; pozunzidwa, tipirira; (1 Akorinto 4:12)

m'zonse tidzitsimikfzira ife tokha monga atumiki a Mulungu, m'kupirira kwambiri, m'zisautso, m'zikakamizo, m'zopsinja, 2 Akorinto 6:4 koma

Potero usacite manyazi pa umboni wa Ambuye wathu, kapena pa ine wandende wace; komatu umve masautso ndi Uthenga Wabwino, monga mwa mphamvu ya Mulungu; (2 Timoteo 1:8)

kuti asasunthike wina ndi zisautso izi, pakuti mudziwa nokha kuti adatiika ife ticite izi., (1 Atesalonika 3:3)

Koma iwe, khala maso m'zonse, imva zowawa, cita nchito ya mlaliki wa Uthenga Wabwino, kwaniritsa utumiki wako. (2 Timoteo 4:5)

Okondedwa, musazizwe ndi mayesedwe amoto adakugwerani inu akhale cakukuyesani, ngati cinthu cacilendo cacitika nanu: koma popeza mulawana ndi

Kristu zowawa zace, kondwerani; kutinso pa bvumbulutso la ulemerero wace mukakondwere kwakukurukuru. (1 Petro 4:12-13)

Muyenera kupirira zowawa ngati msirikali:

Umve zowawa pamodzi nane monga msilikari wabwino wa Kristu Yesu. (2 Timoteo 2:3)

Puulo akufotokozera mwachidule mmene muyenera kuchitira mukakumana ndi chizunzo:

ungakhale umunthu wathu wakunja ubvunda, wa m'kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku. Pakuti cisautso cathu copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero; popeza sitipenyera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. (2 Akorinto 4:16-18)

Paulo akutenge chizunzo ngati chinthu chotitumikira. Iye akufotokoza kuti chizunzo chimatithandiza pamene maso athu alunjika pa mphoto yapachimaliziro osati pa chizunzo kapena vuto lathu.

ZOTSATIRA ZABWINO ZA CHIZUNZO

Zotsatira zabwino malinga ndi chifuniro cha Mulungu ndi izi:

CHIKHULUPIRO CHANI CHIMAYESEDWA:

Chilichonse mudziko lauzimu chimayesedwa. Ichi ndi chifukwa chake mphamvu yachikhulupiro chanu iyenera kuyesedwa:

Ndipo mukamuitana ngati Alate, iye amene aweruzwa monga mwa nchito ya yense, wopanda tsankhu, khalani ndi mantha nthawi ya cilendo canu; (1 Petro 1:17)

chimakhala chiyeso cha chikhulupiro chanu pamene mupemphera ngati Yesu, kuti chikho chachizunzo chimupitirire, koma mapeto ake izi osachitika. Mmallo mwake mumakakamizidwa kumwera chikho chamazuzo. Kom kudzera muchikhukulupiro, timaphunzira kuti sizitanthauza kuti mapemphero athu samayankhidwa koma kuti samayankidwa munjira imene timayembekezera kapena timafuna.

ZIMATHANDIZA KUTI TIKATONTHONZE ATHU ENA:

Wolemekezeka Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Kristu, Atate wa zifundo ndi Mulungu wa citonthozo conse, woo titonthoza ife m'nsautso yathu yonse, kuti tidzathe ife kutonthoza iwo okhala m'nsautso iri yonse, mwa citonthozo cimene titonthozedwa naco tokha ndi Mulungu. (2 Akorinto 1:3-4)

pamene Mupereka chitonthozo cha Mulungu kwa ena:

Mwa ici limbitsani manja ogooka, ndi maondo olobodoka; ndipo lambulani miseu yolunjika yoyendamo mapazi anu, kuti cotsimphinaco cisapatulidwe m'njira, koma ciciritsidwe. (Ahebri 12:12-13)

MUMAPHUNZIRA KUSAKHULUPIRIRA INU MWINI:

Paulo akufotokoza cholinga cha chizunzo chake ku Asiya:

Pakuti sitifuna abale, kuti mukhale osadziwa za cisautso cathu tinakomana naco m'Asiya, kuti tinathodwa kwakukuru, koposa mphamvu yathu, kotero kuti tinada nkhwana ngakhale za moyo wathu; koma tokha tinakhala naco citsutso ca imfa mwa ife tokha, kuti tisalimbike pa ife tokha, koma pa Mulungu wakuukitsa akufa; (2 Akorinto 1:8-9)

Mumayamba kuzindikira kuti:

Koma tiri naco cuma ici m'zotengera zadothi, kuti ukulu woposa wamphamvu ukhale wa Mulungu, wosacokera kwa ife; (2 Akorinto 4:7)

ZIMATHANDIZA KUTI MUKUNZE MAKHALIDWE ABWINO:

Makhalidwe amenewa amakuthandizani kuti mufanizidwe ndi ndi chifaniziro cha Yesu. Ndipo ichi ndiye cholinga cha chikonzero cha Mulungu (Aroma 8:28-29; Ahebri 2:10,18)

NTCHITO ZA MULUNGU ZIMAONEKERA:

Ophunzira a Yesu anafunsa kuti anachimwa ndi ndani ataona munthu wakhungu chibadwireni chake. Iwo anafunsa kuti kodi ndi makolo ake a munthuyo kapena amene anachimwa? Koma Yesu anawayankha nati:

Yesu anayankha, Sanacimwa ameneyo, kapena atate wace ndi amace; koma kuti nchito za Mulungu zikaonetsedwe mwa iye. (Yohane 9:3)

MPHAMVU YA MULUNGU IMAKHALA PA IFE:

Ndipo ananena kwa ine, Cisomo canga cikukwanira; pakuti mphamvu yanga ithedwa m'ufoko. Cifukwa cace makamaka ndidzadzitamandira rriokondweratu m'maufoko anga, kuti mphamvu ya Kristu ikhale pa ine. (2 Akorinto 12:9)

ZINTHU ZONSE ZOSAKHAZIKIKA ZIMACHOTSEDWA PAMOYO WANU:

Zotsatira za chizunzo ndi zakuti zonse zimene ndi zosakhazikika zimachotsedwa pamoyo wanu. Mumasiya kudalira anthu, zinthu zakuthupi kapena zochitika zina ndi zina chifukwa zonsezi zimakhala kuti zakanika nthawi yansautso.

Mulungu akulonjeza kuti:

amene mau ace anagwedeza dziko pamenepo; koma tsopano adalonjeza, ndi kuti, Kamodzinso ndidzagwedeza, si dziko lokha, komanso m'mwamba. Ndipo ici, cakuti kamodzinso, cilozera kusuntha kwace kwa zinthu zogwedezeke, monga kwa zinthu zolengedwa, kuti zinthu zosagwedezeke zikhale. (Ahebri 12:26-27)

Munthawi ya mafunde amoyo, chinachilichonse chimene maziko ake si Mulungu simagwa. (Salimo 119:89 ndi Mateyu 7:24- 27)

CHIDWI CHANU CHA ZOCHITA CHIMASINTHA:

Pamene mwakumana ndi nsautso, nthawi zambiri chidwi chanu chimagona pa chimene chayambitsa komanso zotsatira za nsautso kapena chizunzocho. Koma Mulungu akufuna kuti asinthe chidwi chathu kuti chichoke pa zithu zosakhalitsa ndi ndikukhazikika pa zinthu zamuyaya.

Pakuti cisautso cathu copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero; popeza sitipenyenera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. (2 Akorinto 4:17-18)

Okonedwa, musazizwe ndi mayesedwe amoto adakugwerani inu akhale cakukuyesani, ngati cinthu cacilendo cacitika nanu: koma popeza mulawana ndi Kristu zowawa zace, kondwerani; kutinso pa bvumbulutso la ulemerero wace mukakondwere kwakukurukuru. (1 Petro 4:12-13)

Ngati tipirira, tidzacitanso ufumu ndi iye: ngati timkana Iye, Iyeyunso adzaticana ife: (2 Timoteo 2:12)

CHIKHALIDWE CHATHU CHAKALE CHIMASINTHA:

Mulungu analankhula ndi mtundu wa moabu nati:

Moabu wakhala m'mtendere kuyambira ubwana wace, wakhala pansenga, osatetekulidwa, sananke kundende; cifukwa cace makoleredwe ace alimobe mwa iye, pfungo lace silinasinthika. (Yeremiya 48:11)

Chifukwa chakuti anthu aku moabu anali asanakumane ndi msautso kapena chiyesero cha chikhulupiriro chao, iwo sanali anthu osinthika. Iwo anakhala moyo otayilira ndipo anakhazikika pachuma chao. Sanakule muuzimu ngati mtundu wa anthu ndipo panalibe kusinthika kwina kulikonse pakati pao. Ndipo fungo lao lakale anali nalobe. Fungo la Moabu linali losasinthika.

Mazunzo amathandiza kuchotsa chikhalidwe chakale. Pamene mukutakwidwa, kukumana ndi mavuto a moyo, fungo lanu lachikunja limasinthika ndipo mumayamba kumveka fungo lauzimu.

MULUNGU AMAKHALA AKUKONZEKERETSANI UTUMIKI:

Ngati mukufuna kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu, kapena mufuna kufananizidwa ndi Yesu Khristu ndikukhala chotengeramo chake, Mulungu akhoza kuyankha zonsezi pogwiritsa ntchito chizunzo kapena nsautso.

**Taona ndakuyenga, koma si monga siliva, ndakuyesa iwe m'ng'anjo ya masautso.
(Yesaya 48:10)**

Kudzera muchizunzo kapena nsautso, mumachoka pongakhala mwana wa Mulungu ndikukhala osankhidwa wake wa Mulungu. Mazuzo obwera chifukwa cha chifuniro cha Mulungu anakukonzekeretsani kuti mukagwire ntchito moyenera.

MUMAKONZEKERETSEDWA KUTI MULAMULIRE NDI KHRISTU:

**Ngati tipirira, tidzacidanso ufumu ndi iye: ngati timkana Iye, Iyeyunso adzatikana ife:
(2 Timoteo 2:12)**

MAZUNZO AMABWERETSA MADALITSO AUZIMU:

Yesu anati:

**Odalaaliakuzunzidwacifukwa ca cilungamo: cifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba. Odala muli inu m'mene adzanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa ziri zonse cifukwa ca Ine. Sekerani, sangalalani: cifukwa mphotho yanu ndi yaikuru m'Mwamba: pakuti potero anazunza aneneri anakhalawo musanabadwe inu.
(Mateyu 5:10-12)**

MUMAPHUNZIRO KUMVERA KUDZERA MUMAZUNZO:

**Angakhale anali Mwana, anaphunzira kumvera ndi izi adamva kuwawa nazo;
(Ahebri 5:8)**

MAU A MULUNGU AMAYESEDWA MKATI MWANU:

Mau a Yehova ndi mau oona; Ngati siliva woyenga m'ng'anjo yadothi, Yoieretsa kasanu ndi kawiri. (Masalmo 12:6)

MAZUNZO AMATITHANDIZA KUTI TIDZICHEPETSE:

Amene anakutsogolerani m'cipululu cacikuru ndi coopsaco, munali njoka zamoto, ndi zinkhanira, mouma mopanda madzi; amene anakuturutsirani madzi m'thantwe lansangalabwi; amene anakudyetsani m'cipululu ndi mana, amene makolo anu sanawadziwa; kuti akucepetseni, ndi kuti akuyeseni, kuti akucitireni cokoma potsiriza panu; (Deuteronomo 8:15-16)

MAZUNZO AMAPANGITSA KUTI MUKULE:

Pakufulua ine muniyankhe, Mulungu wa cilungamo canga; Pondicepera mwandikulitsira malo: Ndicitireni cifundo, imvani pemphero langa. (Masalmo 4:1)

MUMAKHALA CHIFUPI NDI MULUNGU:

Mazunzo amathandiza kuti mukhale ndi ubale waukulu ndi Mulungu. Atakumana ndi nsautso waukulu, Yobu anazindikira choonadi chimenechi. Ndipo anati:

Kumva ndidamva mbiri yanu, Koma tsopano ndikupenyani maso; Cifukwa cace ndekha ndidzinyansa, ndi kulapa M'pfumbi ndi mapulusa. (Yobu 42:5-6)

Ambiri mwa ife timamudziwa Mulungu mwapamwambamwamba. Pamene zinthu zikuyenda Mulungu samakhalanso ofunika pamoyo wathu. Koma zinthu zikayamba kuvuta ndi pamene Mulungu amakhala ofunikira pamoyo wathu. Yobu anamudziwa Mulungu mozama pamene anakumana ndi nsautso. Izi sizikutanthauza kuti iye samamamudziwa Mulungu ayi, koma kumidziwa kwake kunali kungokhala ndi chidziwitso chabe cha Mulungu. Koma iye atakumana ndi nsautso, anamudziwa Mulungu kudzera munyengo zimene anadutsamo.

Paulo nayenso akufotokoza mfundo yomweyi:

Kuti ndimzindikire iye, ndi mphamvu ya kuuka kwace, ndi ciyanjano ca zowawa zace, pofanizidwa ndi imfa yace; (Afilipi 3:10)

Mukhodza kudziwa Mulungu kudzera muchiyanjano cha chizunzo.

Munyengo yonse yansautso wake, Yobu amafunsa Mulungu mafunso. Iye amaona ngati kuti gwero lan nsautso wa wake linali Mulungu. sikutu ndi zolakwika kufunsa Mulungu mafunso. Mwachitsanzo, ngakhale kuti Yesu amadziwa kuti cholinga chake chobwelera pa dziko lapansi chinali kudzapulumutsa munthu kumachimo, koma utafika nsautso, iye anafula nati, Mulungu wanga Mulungu wanga, mwandisiranji? Mau amene analakhula litatha funso limeneli ndi amene ali ofunika kwambiri chifukwa iye anati “mzimu wanga ndiupereka mmanja mwanu”

Ngakhale kuti Yobu anali ndi mafunso, koma iye anati:

Iye adzakhalanso cipulumutso canga, Pakuti wonyoza Mulungu sadzafika pamaso pace. (Yobu 13:16)

Koma ndidziwa kuti Mombolo wanga ali ndi moyo, Nadzauka potsiriza papfumbi. Ndipo khungu langa litaonongeka, Pamenepo wopanda thupi langa, ndidzapenya Mulungu; (Yobu 19:25-26)

Mafunso onse atatha, Yobu anachoka pakhazikika pa “iye” ndikukhazikika pa “Inu.” Muyenera kupereka nsautso wanu komanso mafunso onse osayankidwa mmanja mwa Mulungu.

Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, Osacirikizika pa luntha lako; (Miyambi 3:5)

Mulungu amaonetsera pang'ono cholinga cha nsautso wanu, koma ndi zotheka kuti simungathe kumvetsa chinachilochonse.

Kubisa kanthu ndi ulemerero wa Mulungu; (Miyambi 25:2)

Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (Deuteronomo 29:29)

Pali zinthu zina zobisika zimene ndi za Mulungu yekha. Ndipo ngati Yobu, mwina simungathe kumvetsa cholinga cha nsautso wanu.

Yehova alongosola mayendedwe a mwamuna; Munthu tsono angazindikire bwanji njira yace? (Miyambi 20:24)

Pamapeto azonze Mulungu atalankhula ndi Yobu pogwiritsan tchito zitsanzo zachilengedwe zimene Yobu sanathe kufotokozer. Mfumdo imene Mulungu amatsindika ndi yakuti ngati yobu samveta zitsanzo zakuthupi zimene ndi zooneka ndi maso, iye sakanamvetsa zinthu zosaoneka ndi maso za dziko lauzimu. Yobu atakumana ndi Mulungu, zinali zopanda ntchito kuti mafunso ake analibe mayakho. Nkhawa zonse zobwera chifukwa chakuganiza kwa umuthu zinamuthera. Mayankho amafunso ake anali chikhulupiriro.

Pamene mwamudziwa Mulungu mwakuya kudzera muchizunzo, mumadziona mmene muyenera kudzionera. Zotsatira zokumana ndi Mulungu maso ndi maso zomakhala zoposa mafuso onse ndi kukambirana kungachite.

Pamene Yobu anafika pamaso pa Mulungu, panalibe yankho lina lilironse limene anakanapereka. Iye apatsidwa choonadi china chokhudza chizunzo. Mafunso ake onse anakhala opana kathu pamaso pa Mulungu ndipo panalibeso kukaika kwina kulikonse kumene anakhala nako.

NAMONDWE WAMOYO

Chizunzo nthawi zina chimafanizidwa ndi namondwe. Pamene mukumana ndi chizunzo, mumakhala kuti mwakumana ndi namondwe muuzimu. Ndipo izi zimakhudza moyo wanu kuthupi, kuuzimu ngakhale maganizidwe anu amene.

Baibulo limafotokoza za namondwe amene ophunzura anakumana naye. Werengani nkhani imeneyi pa Marko 4:35-41. Namondwe amaneyu anali nkondo yochokera kwa Satana. Yesu anauza ophunzira kuti apite tsidya lina lanyanja. Koma Satana amafuna kuwarepheretsa kupita tsidya lina chifukwa cha zozizwa zimene zimayenera kuchitika dera limene iwo amapita (Marko 5) Koma Yesu anaonetsera ulamuliro pa namondwe amaneyu pamene anadzudzula mphamvu ya mdaniyo. Bata linabweleranso panyanja ndipo iwo anapitiriza ulendo wao popanda chovuta china chilichonse.

Namondwe wa Satana ndi china chilichonse chimene chimakulepheretsani inu kukwaniritse chifuniro cha Mulungu pamoyo wanu. Izi sizimabwera chifukwa chakuti mwachimwa kapena kuti mwasephana ndi chifuniro cha a Ambuye. Pamene mwakumana ndi mavuto ngati amenewa

muyenera kugwiritsa ntchito ulamuliro wanu pa mdani wanuyo. Yesu watipatsa ulamuliro pa mphamvu ina iliyonse ya mdani.

Pali nkhani ziwiri za namondwe wakuthupi zimene zikuonetsera chizunzo ngati zotsatira za uchimo komanso chizunzo ngati chifuniro cha Mulungu. Werengani nkhani ya Yona pa Chaputala Ikomanso ya Paulo pamachitidwe 27. Ndipo gwiritsani ntchito chithunzi chili pansichi.

Yona

Yona anadziika yekha mu namondwe ake

Iye analipire ndalama kuti ayende panyanja

Iye anali choyambitsa nomondweyo

Analibe mdalitso wa Ambuye

Oyendetsa ngalawayo anali ndi mantha

Kuti apulumutsidwe:

Yona amayenera kuponyedwa mmadzi

Paulo

Paulo sanagwe munamondwe chifukwa cha vuto

Iye anawaretsa kuti asayende panyanja

Anali yankho osati choyambitsa

Anali ndi mdalitso wa Mulungu

oyendetsa ngalawayo anali ndi nsangara.

Kuti apulumutsidwe:

Onse amayenera kukhala mungalawoyo.

Pali kusiyana pakati pakukumana ndi namondwe chifukwa cha chifuniro cha Mulungu ndi kukumana ndi namondwe chifukwa chakuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Ngati mukumana ndi namondwe chifukwa chakuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu, iyi ndi nyengo imene mumachita kuipanga nokha. Mwachitsanzo, okhulupilira amene wakwatira munthu osakhulupirira amakumana ndi mavuto chifukwa chakuti wasemphana ndi mfundo za Baibulo.

Pamene mwayambitsa namondwe pamoyo wanu, mumakhala kuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu ndipo simukumvera Malamuro ake. Nthawi zambiri simumadziwa kukula kwa zotsatira za nyengo yanu. Mumakhala kuti mwagona pamene namondwe amakhala akukulirabe pakati panu. Mdalitso wa Mulungu sumakhala nanu ndipo onse okuzungulirani amakhanso amatha. Namondwe ameneyu si nkondo yochokera kwa Satana ayi, koma ndi chidzudzero chochokera kwa Mulungu amene amakukondani ndipo akufuna kuti mubwelerenso ndikuyamba kuchita chifuniro cha Mulungu. Mukhoza kulengeza malonjezano amphamvu pamdaniyo, koma izi sizimasintha nyengo zanu.

Pamene mwazindikira kuti nyengo yanu yachizunzo ikubwera chifukwa cha tchimo, choyenera kuchita ndi kupempha Mulungu kuti atikhululukire.

Pamene mukumana ndi nsautso chifukwa cha chifuniro cha Mulungu, nyengo yake imakhala yosiyana. Izi zimachitika osachiti chifukwa chakuti mwachita tchimo kapena kuti mwalakwitsa ayi. Inuyo mumakhala yankho ku vuto limene lakuzungulirani. Ngati Paulo, mukhoza kutenga ulamuliro wauzimu chifukwa mdalitso wa Mulungu uli pa inu komanso mukhoza kulimbikitsa anthu ena chifukwa ndinu yankho ku namondwe osati choyambitsa cha namwodweyo. Simuyenera kutsika ngalawa chifukwa chothawa nsautso. Koma muyenera kukhala mungalawa yansautso chifukwa ndi chifuniro cha Mulungu.

MSILIKARI OKUMANA NDI CHIZUNZO

Pamene mukumana ndi chizunzo muyenera kuzindikira kuti simuli nokha ayi:

**Podziwa kuti zowawa zomwezo zirimkukwaniridwa pa abale anu ali m'dziko.
(1 Petro 5:9)**

Namodwe pamoyo wa munthu ndi chinthu chosathawika ndipo ndi zovuta kupewa. Chitsanzo chabwino cha mfundo imeneyi ndi Mateyu 7:24-27. Nsautso kapena chizunzo zimabwera pa anthu amene moyo wao wamangika pa Mulungu komanso ngakhale iwo amene sanatero. Koma maziko a mayo wa munthu ndi amene amaonetsera zotsatira za namondwe pamoyo.

Tiyenera kuyembekezera chizunzo ngati mbali imodzi ya chifuniro cha Mulungu:

Ndipo onse akufuna kukhala opembedza m'moyo mwa Kristu Yesu, adzamva mazunzo. (2 Timoteo 3:12)

kuti kwapatsidwa kwa inu kwaufulu cifukwa ca Kristu, si kukhulupirira kwa iye kokha, komatunso kumva zowawa cifukwa ca iye, (Afilipi 1:29)

. . . kuti mu-kawerengedwe oyenera ufumu wa Mulungu, umenenso mumvera zowawa; (2 Atesalonika 1:5)

Pakutinso, pamenetinali ndi inu tinakuuziranitu kuti tidzamva zisautso; monga kudacitika, monganso mudziwa. (1 Atesalonika 3:4)

Pamenepo adzakuperekani kunsautso, nadzakuphani; ndipo anthu a mitundu yonse adzadana nanu, cifukwa ca dzina langa. Mateyu 24:9

Koma zisanacitike izi, anthu adzakuthirani manja, nadzakuzunzani, nadzapereka inu ku masunagoge ndi ndende, nadzamuka nanu kwa mafumu ndi akazembe, cifukwa ca dzina langa. (Luka 21:12)

Kumbukilani mau amene Ine ndinanena kwa inu, Kapolo sali wamkuru ndi mbuye wace. Ngati anandilondalonda Ine, adzakulonda-londani inunso; ngati anasunga mau anga, adzasunga anunso. (Yohane 15:20)

Koma izi sizikutathuaza kuti muchite kupangira dala kuti mukumane ndi chizunzo ndi cholinga chofuna chokongweretsa Mulungu. Mulungu samakondwera pamene anthu akumana ndi

chizunzo. Kuchita kupangira dala kuti mukumane ndi chizunzo ndi tchimo pamaso pa Mulungu. Anthu amene amachita kufuna chizunzo, kumakhala kufuna kudziyenera pamaso pa Mulungu komanso kufuna kuoneka oyera pamaso pa anthu. Koma Mulungu amakondwera ndi mwazi wa Yesu Khristu wokha. Koma Mulungu amakhudzika ndi chizunzo cha moyo wathu ndipo iye amatha kugwiritsa ntchito izi ndi cholinga chabwino pa moyo wathu.

Mbali imodzi yophunzitsa anthu ongobadwa kumene mumpingo oyamba wa atumwi inali kuwaphunzitsa kuti adzakumana ndi nsautso. Ichi ndi chinthu chimene tikusemphana nacho mu mpingo wa lero.

Nalimbikitsa mitima ya akuphunzira, nadandauliraiwo kuti akhalebe m'cikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu ndi zisautso zambiri. (Macitidwe 14:22)

Yesu akuitana onse omutsata iye kuti adzikanize okha:

Ndipo anadziitanira khamulo la anthu pamodzi ndi ophunzira ace, nati kwa iwo, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wace, nanditsate Ine. (Marko 8:34)

Ndipo iye ananena kwa onse, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wace tsiku ndi tsiku, nanditsate Ine. (Luka 9:23)

Ndipo amene ali yense sasenza mtanda wace wa mwini yekha, ndi kudza pambuyo panga, sakhoza kukhala wophunzira wanga, (Luka 14:27)

Pamene mukumenya nkondo yauzimu sizimatanthauza kuti mumakhalira chipambano chokhachokha ndi chikondwewero. Ngati muli nsirikali wa Mulungu, muyenera kupilira chizunzo:

Msilikari sakodwa nazo nchito wamba, kuti akakondweretse iye amene adamlemba usilikari. (2 Timoteo 2:4)

Mfundo ina imene imagwiritsidwa ntchito pomenya nkondo zakuthupi ndi yakuti sumasiya kumenya nkondo chifukwa chakuti mwavulara”

KUYENDERA PERETE

1. Lembani Vesi yotsogolera osonera.

2. Kodi chizunzo chinabwera bwanji pa dziko lapansi?

3. Tchulani njira zisanu zimene chizunzo chimabwelera pa moyo wa munthu okhulupirira

4. Tchulani zotsatira zitatu zabwino zokumana ndi chizunzo

5. Fotokozerani mfundo zitatu zamaonedwe oyenera a chizunzo.

6. Werengani ziganizo zili munsimuzi. Ngati chiganizo chili cholondora, lembani T. Ndipo lembani F kutsogolo kwachiganizo ngati chili chosalondola.

- a. ___ Sichifuniro cha Mulungu kuti mukumane ndi chizunzo.
- b. ___ Ngati mukukumana ndi mmavuto zimakhala kuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu.
- c. ___ Paulo anali atasemphana ndi chifuniro cha Mulungu pamene anakumana ndi namondwe panyanja.
- d. ___ Pamene tikumana ndi chizunzo chifukwa chosemphana ndi chifuniro cha Mulungu, gwero la vuto lathu kumakhala kuti sitinamvere Mulungu.

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

MACHITACHITA ALUSO

1. Kodi mukukumana ndi chizunzo pakadali pano? Unikirana zifukwa zimene anthu amakuna ndi chizunzo malinga ndi chaputal ichi.
 - Anthu ena okunzungulirani
 - Nyengo za moyo.
 - Utumiki wanu.
 - Nkhondo yochokera kwa Satana
 - Machimo anu.

Kodi ndi chifukwa chiti chimene mukukumana ndi ndi chizunzo. Ngati mukumana ndi chizunzo chifukwa chakuti mwachimwa, choyenera kuchita ndi kungolapa basi. Koma ngati mukumana ndi chizunzo chifukwa cha anthu ena, nyengo za moyo, kapena chifukwa cha nkhondo za moyo, kodi cholinga cha chizunzo chimenechi chikhoza kukhala chiani?

2. Unikirani ubwino okumana ndi chizunzo umene watchulidwa pansipa. Ndipo pezani cholinga chimene mukuona kuti Mulungu akufuna akwaniritse pa moyo wanu. Kenako chitani zinthu malingana ndi nyengo imeneyi.
 - Chikhulupiriro chanu chimayesedwa.
 - Mumakonzekeretsedwa kuti mutonthoze anthu ena.
 - Muphunzire kusakhulupirira inu mwini.
 - Mumakuza chikhalidwe chabwino chauzimu.
 - Ntchito za Mulungu zimaonekera.
 - Mphamvu ya Mulungu imaonekera.
 - Zinthu zonse zosakhazikika zimachotsedwa.
 - Chidwi chanu cha moyo chimasintha.
 - Chikhalidwe chanu chakale chimasinthika.
 - Mumakonzekeretsedwa pa utumiki.
 - Mumakonzekeretsedwa kuti mulamulire ndi Khirustu Yesu.
 - Mumalandira madalitso auzimu.
 - Muphunzire kumvera.
 - Mau a Mulungu amayesedwa mkati mwanu.
 - Mumphunzira kudzichepetsa.
 - Mumakuzidwa moyo wanu wauzimu.
 - Ubwenzi wanu ndi Mulungu umakula.
3. Pa nkhondo yakuthupi, asilikari amathandizana wina ndi mzake. Pamene msilikari wazingidwa ndi adani, asarikari ena amabwera kudzathandizira kuti msilikari nzao athe kuthawa. Kodi alipo mnsirikali mzanu amene mukudziwa kuti wavulala ndipo inuyo mukhoza kumuthandiza kuti apeze mwayi othawa? Kodi mukhoza kuthandiza anthu ena pa nkhondo yauzimu poima nao mupemphero komanso ndi kuwalimbikitsa?
4. Werengani zambiri zokhudza chizunzo mu buku la 1 Petro.
5. Werengani mavesi amene akukamba zokhudza chizunzo:

Nyengo zolimba: II Timoteyo 2:3.

Zowawa/ Machitidwe 14:20; Aroma 5:3; 12:12; I Atesalonika 3:4, II Tesalonika 1:4
Chizunzo; I Petro 5:10-12, 44; 13:21; Marko 4:17; Luka 11:49; 21:12; Yohane 15:20; I
Akorinto 4:12; II Akorinto 4:9; Machitidwe 8:1; 11:19; 13:50; II Timoteyo 3:12; Aroma
8:35; Agalatiya 6:12.

Nsautso: Salimo 34:19; 119:67, 71, 75; Mateyu 24:9; Machitidwe 20:23; II Akorinto 2:4;
4:17; 6:4; I Atesalonika 3:3; II Timoteyo 1:8; 3:11, 4:5; II Akorinto 1:6; Yakobo 5:10;
Ahebri 10:32-33.

CHAPUTALA 23

KUGONJA PA KUMENYANA KOMA NDI KUPAMBANA NKHONDO

ZOLINGA:

Pamapeto pamaphunziro awa, muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsolera osaonera.
- Kupeza zitsanzo za anthu amene agonjetsedwa pakumenyana koma ndi kupambana pa nkhondo.
- Kutchula njira zinayi zoti mupambane nkhondo ngakhale mutagonjetsedwa pakumenyana.
- Kupereka ma vesi amene mutha kugwiritsa ntchito pamene Satana afuna kukuweruzani ngati olemphera.
- Kufotokozerana zomwe mungaphunzire pakulephera kwanu muuzimu.

VISI YOTSOGOLERA YOCHKERA MUZOLEMBA ZAUZIMU.

Ndalimbana nako kulimbana kwabwino, ndatsiriza njirayo, ndasunga cikhulupiriro: (2 Timoteo 4:7)

MAU OYAMBA.

Muphunziro limeneli mwaphunzira ukadauro wa kamenyedwe ka nkhondo yauzimu. pamene mungagwiritse ntchito ndi mfundo zimenezi, zikuthandizani kuti mukule mukuthekera kwanu kotha kumenya nkhondo yauzimu ndi mphamvu ya ambuye wathu Khristu Yesu. Posatengera kuti muli ndi chidziwitso komanso ukadaulo wa nkhondo yauzimu, muzimukumanabe ndi zolempheleletsa nthawi ndi nthawi. Koma simukuyenera kutaya mtima chifukwa ma atumiki ena amphamvu anakumana ndi nyengo zofanana ndi zimene mukukumana nazo.

KUGONJETSSEDWA PA KUMENYANA

Pali zitsanzo za nthu ambiri mu Baibulo amene agonjetsedwa ndi mdani:

YOSWA

Yoswa anali otsogolera nkhondo wamkulu amene anatenga utsogoleri wa fuko la Israeli Mose atamwalira. Chinthu chimodzi chovuta chimene Yoswa ameyenera kuchita kunali kuwatsogolera ana a Israeli kuti awoloke mtsinje wa Yorodani ndi kulowa mu dziko lamalonjezano. Koma m' modzi wa ankhondo a Israeli anachimwa pamene anatenga katundu oletsedwa pamene amagonjetsa adani awo. Chifukwa chakuti panali tchimo pakati pa ana a Israeli, iwo anagonjeseza pakumenyana kumene kunachitika mu mzinda wa Ai (Yoswa 7).

Mfumu Davide agonja pakumenya kumene kunachitika pa iye ndi Mfumu a Amaleki amene anagonjetsa chigawo chakumwera kwa ufumu wa Davide ndikuotcha mzinda wa Zikilagi. Iwo anagwira ukapolo azimayi komanso ndi azikazi a mfumu omwe. Chifukwa cha ichi, abwenzi a

Davide komanso ndi asirikari ake omwe anali osakodwa kotero kuti amkafuna kumupha pomugenda miyala. Davide anali wankhawa ndi okhumudwa chifukwa cha izi (I Samueli 30:1-6)

Mfumu Davide inagonjanso nkhondo yaikulu yauzimu. Iye anachita chigololo ndi mkazi wa mwini. Koma chifukwa chakutu Bateseba anatenga pakati, Davide anaganiza zoti aphe mamuna wake ndi cholinga chofuna kubisa tchimo lake. (I Samueli 11-12)

MNENERI ELIYA

Mfumuakazi yoipa yotchedwa Jezebeli inatumiza nthumwi kwa Eliya kuti amudziwitse iye kuti wakonza chikonzero kuti aphedwe:

**... Koma iye mwini analowa m'cipululu ulendo wa tsiku limodzi, nakakhala pansi patsinde pa mtengo watsanya, napempha kuti afe; nati, Kwafikira, cotsani tsopano moyo wanga, Yehova; popeza sindiri wokoma woposa makolo anga.
(1 Mafumu 19:4)**

Komatu iye anali munthu waphamvu wa Mulungu amene ali atapanga zodabwitsa monga kuchiritsa anthu odwala, kuukitsa anthu akufa ngakhale kulamula chilengedwe chimene mu dzina la Mulungu. Ngakhale anapanga zinthu izi, iye anali kubisala, opanda chiyembekezo. Kotero kuti amangodikira nthawi yake ya imfa.

MTUMWI PAULO:

Mtumwi Paulo naye anakumana ndi kugonjedwa. Iye akufotokoza kuti anathodwa kwakulu kuposa mphamvu zake komanso anada nkhwana ngakhale za moyo wake (2 Akorinto 1:8). Ndipo panali nyengo zina zimene iye anali osautsika, ozunzidwa, wamantha ndi othodwa (2 Akirinto 4:8-11; 7:5-6)

KUNGONJETA PA NKHONDO

Mtsogoleri wina aliyense amene watchulidwa, anagonjapo pakumenya ndi mdani. Chimodzimodzi nanunso pamene mukumenya nkhondo yauzimu, mukhoza kukumana ndi kugonjetsedwa. Koma ngakhale kuti mukhoza kugonja pakumenyana, izi sizikutnthauza kuti ndiye kuti mwagonja nkhondo. Nkhondo imakhala ndi kumenya kungapo. choncho, chifukwa chakuti mwagonja pakumenyana sizikutanthauza kuti mwagonjetsedwa pa nkondo.

Anthu onsewa amene anagonja pakumenyana, anayimabe ndipo mapeto ake anapambana nkhondo. Njira zauzimu zimene anagwiritsa ntchito zikuthandizani pamene mwagonjetsedwa pakumenyana. Ndi zotheka kuimabe ngakhale munakodwa pa nsampha wa nkhondo ya Satana.

ndipoakadzipulumutse ku msampha wa mdierekezi, m'mene anagwidwa naye, ku cifuniro cace. (2 Timoteo 2:26)

Mau akuti kuchira amatanthauza kudzukanso. Pamene nsampha ndi chithu chobisika chimene cholinga chake ndi kukola chinachake. Kuti muchirenso kapena kubweleranso mutangonjetsedwa pakumanyana, zina mwa ndondomeko zimene muyenera kutsata ndi izi:

NJIRA YOYAMBA: KUZINDIKIRA KULEPHERA KWANU.

Yoswa anazindikira ndi kuvomereza kulephera pa mzinda wa Ai. Ndipo iye anati:

**Ndidzanenanji, Ambuye, Israyeli atabwerera m'mbuyo pamaso pa adani ao?
(Yoswa 7:8)**

Kunali kosavuta kwa Davite kuti avomereze kulakwitsa kwake pa zimene zinachitika ndi mzinda wa Zikilagi. Zinali zoonekeratu ndi wina aliyense kuti anagonjetsedwa. Koma zinali zovuta kwa Davide kuti avomereze tchimo lake la chigolo ndi Beteseba. Panalibe amadziwa tchimo limeneli kupatuala iye, Beteseba, ndi mneneri wa Mulungu. Koma Davide anavomereza kuti wachimwira Mulungu (II Samueli 12:3)

Eliya anavomereza kulephera kwane. Ndipo anati:

Kwafikira, cotsani tsopano moyo wanga, Yehova; popeza sindiri wokoma woposa makolo anga. (1 Mafumu 19:4)

Nayenso Paulo anavomereza kulephera kwake (II Akorinto 4:8-9, II Akorinto 1:8). Simukuyenera kukanika kuvomereza kuti mwagonjetsedwa pa kumenyana. Ndi cholinga choti muchoke pakugonjako, muyenera kuvomereza kuti mwagonja.

**Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi.
(1 Yohane 1:8)**

NJIRA YACHIWIRI:

Kuvomereza kokha kuti mwagonja sikokwanira. Muyeneranso kupempha Mulungu kuti akukhululukireni:

**Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutsambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse.
(1 Yohane 1:9)**

- Davite analapa tchimo limene anachita ndi Beteseba. Mukhoza kuwerenga pemphero lakulapa limene Davite anapemphera pa Salimo 52. Ili ndi Salimo labwino kugwiritsa ntchito pamene mwalephera.
- Yoswa anaunguza mpaka atapeza chimene chinapangitsa kuti agonje pa mzinda wa Ai. Iye anazindikira kuti kusamvera pakati pa atsogoleri ankhondo kunapangitsa iwo kuti agonje. Iye ndi anthu onse analapa pamaso pa Mulungu.

- Eliya nayenso alapa chikwa iye anazindikira kuti anali wagwiro kusiyana ndi m'bado wamakolo ake (I Mafumu 19:4)
- Paulo anaonetsea kuti ngakhale anali ndi nkondo yaikulu ndi thupi, koma iye anapeza chipambano kudzera mukulapa ntchito zakufa (Aroma 8; Ahebri 6:1)

NJIRA YACHITATU: MANGANINSO MPHAMVU ZANU ZAUZIMU:

Kudziko lakuthupi, pamene asirikali agonjetsedwa, pamatenga nthawi kuti abwerenso pamodzi ndi cholinga choti abwelere kunkhondo. Atsogoleri ankhondo amayamba kaye aunikira zinthu zolakwika, kukonza zolakwikazo komanso ndi kuwalimbikitsa asirikali anasabwelerenso kunkhondo. Iyi ndi mfundo yofunika kwambiri mu dziko lauzimu. Pemene mwakumana ndi kulephera pa nkondo yauzimu, chimene muyenera kuchita ndi kumanganso mphamvu zanu zauzimu.

- Yoswa anadikira mupemphero kuti mphamvu zake zauzimu zibwelere asanakamenyenso nkondo. Iye anapemphera kuti azindikire chifukwa chimene analephelera komanso kuti apezec chitsogozo chokonzera zinthu zimene zinalakwika (Yoswa 7:6-15).
- Davide anapemphera ndi kusala chakudya chifukwa cha tchimo lake ndi Beteseba. Patapita nthawi, iye analandira chakudya chakuthupi chimene anasiya kudya mwana wake ndi Beteseba atamwalira.
- Eliya anapuma, anatumikiridwa ndi angelo, kenako anadikira paphiri kufikira nthawi imene analandiranso mphamvu ya Mulungu (I Mafumu 19)
- Paulo anadzilimbikitsa yekha mwa ambuye. Iye anazindikira kuti palibe china chilichonse chimene chingamulekanitse ndi chikondi cha atate ngakhale kulephera kumene:

Adzatisiyanitsa ndani ndi cikondi ca Kristu? nsautso kodi, kapena kupsinjika mtima, kapena kuzunza, kapena njala, kapena usiwa, kapena zoopsya kapena lupanga kodi? Koma 13 m'zonsezi, ife tilakatu, mwa iye amene anatikonda. ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale colengedwa cina ciri conse, sicingadzakhoze kutisiyanitsa ife ndi cikondi ca Mulungu, cimene ciri mwa Kristu Yesu Ambuye wathu. (Aroma 8:35,37,39)

Zina mwa njiri zimene mungagwiritse ntchito kuti mubwenzeretse mphamvu zanu ndi izi:

- Werengani buku loposa mabuku onse limene ndi ... Mau a Mulungu. Pezani nthawi yoti mupephere ndi kusala chakudya. Pamene muchita izi, gwiritsani mfundo zapephero ndi kusala kudya zimene mwaphunzira muphunziro limeneli.
- Pemphani Mulungu akuonetsera chimene chapangitsa kuti mulephere komanso chimene mungachite kuti mukonze zolepherazo.

- Unguzanizo ndondomeko za Nkhondo yauzimu mu phunziro limeneli. Pemphani Mulungu kuti akupatseninsu mphamvu zanu ndi kukuthandizani kuti mugwiritse ntchito ndondomeko zimene zalembedwa mu buku ili.
- Muyenera kupuma kuthupi chifukwa munthu ali mu magawo awa: thupi, moyo ndi mzimu. Choncho ngati thupi lanu liri lofooka, Satana akhoza kutengerapo mwayi kuti alimbane ndi mzimu ndi moyo wanu.

NJIRA YACHINAYI: BWELERANINSO KUNKHONDO:

Njira imodzi imene m'dani wanu amagwiritsa ntchito kufuna kukuyesani ndi ya kuti mungosiya kumenya nkhondo pamene mwaluza kumenyana muuzimu. Inde ndi zoona kuti Mzimu Woyera adzakutsutsani pamene mwalephera koma pali kusiyana pakati pa kutsutsidwa ndi Mzimu Woyera ndi chiweruzo chochokera kwa m'dani. Pamene mwachimwa, Mzimu Woyera amakuuzani chimene mwalakwitsa, pamene Satana samatchula mwatchutchu chimene mwalakwitsa iye amangokuweruzani.

Chimene Satana amachita ndi kulankhula mosalunjika pofuna kukugonjetsani:

- “mukhoza kungosiya”
- Wina aliyense anasiya kukukhulupirirani.
- Mulungu samasala zainu chifukwa akanatha kukuthandizani inu.
- Ndinu ofooka ndipo palibe chabwino mwainu.
- Simungakwanitsenso kukhala okhulupirira.
- Si inu abwino.

Simukuyenera kuvomereza chiweruzo cha m'daniyu. Mukungoyenera kuvomereza kulephera kwanu, kulapa pamaso pa Mulungu ndi kuzindikira kuti:

Cifukwa cace tsopano iwo akukhala mwa Kristu Yesu alibe kutsutsidwa. (Aroma 8:1)

Gwiritsani ntchito vesi imeneyi kuti mugonjetse chiweruzo cha Satana komanso kuti mubwelerenso kunkhondo.

- Yoswa anapitirizabe kumenya nkhondo ndipo anapambana mu dziko lamalonjezano. Iye anabwelera kunzinda wa Ai ndikugonjetsa adani amene anamugonjetsa pachiyambi. Pamene mwabwelera kunkhondo yauzimu., simungotenga zokhazo zimene adani anu analanda, koma mumapitirabe kugonjetsa munkhondo zina.
- Pamene Davide anagonjetsedwa mu khondo ya ku Zikilagi, iye anabwelera ku nkhondo ndi kuyamba kugonjetsa munkhondo zina. Iye anakwanitsa kubwenzera zonse zimene a Amaleki anatenga:

Ndipo Davide analanditsa zonse anazitenga Aamaleki, napulumutsa akazi ace awiri. Ndipo sikanasoweka kanthu, kakang'ono kapena kakakuru, ana amuna

**kapena ana akazi, kapena cuma kapena dna ciri conse ca zija anazitenga iwowa;
Davide anabwera nazo zonse. (1 Samueli 30:18-19)**

Naye Eliya anakwanitsa kugonjetsa kugwira njakata kwake nabwelera kukamenya nkondo yauzimu. Iye anakwanitsa kutchita zodabwitsa zazikulu kwambiri mu mbiri yautumiki.

Ikakhala nkhani ya Paulo, mukhoza kuwerenga ndime imene tinatchula kale ija.

**Ndife osautsika monsemo, koma osapsinjika; osinkhasinkha, koma osakhala kakasi;
olondoleka, koma osatayika; ogwetsedwa, koma osonongeka; (2 Akorinto 4:8-9)**

Iye anali wankhondo wamphamvu ogonjetsa. Iye anati:

osautsika, KOMA OSAPSINJIKA;

osinkhasinkha, KOMA OSAKHALA KAKASI;

olondoleka, KOMA OSATAYIKA;

ogwetsedwa, KOMA OSAONONGEKA;

KUPHUNZIRA KUCHOKERA MUKULEPHERA.

Paulo anelemba ku Akorinto:

**Ndife osautsika monsemo, koma osapsinjika; osinkhasinkha, koma osakhala kakasi;
olondoleka, koma osatayika; ogwetsedwa, koma osonongeka; (2 Akorinto 4:8-9)**

Paulo akufotokoza kuti mavuto amene anakumana nao kwa Asiya anamuphunzitsa phunziro lalikulu. Phunziro ndi lakuti, Sitiyenera kudzikhulupirira tokha ayi. Ili ndi phunziro lalikulu limene tiyenera kuphunzira pamene talephera. Simungadzidalire nokha pamene mumenya nkondo yauzimu. Ulamuliro wanu ndi chipambano chanu zili mwa Khristu Yesu yekha basi.

Paulo amaona zinthu kupyora maonedwe a dziko lapansi ndi cholinga choti aone ubwino wauzimu umene mavuto, chiyeso ndi zina zimabweleretsa.

**Cifukwa cace sitifoka; koma ungakhale umunthu wathu wakunja ubvunda, wa
m'kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku. Pakuti cisautso cathu
copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa
ulemerero; popeza sitipenyenera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti
zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. (2 Akorinto
4:16-18)**

Paulo anazindikira kuti ngakhale munthu wakunja amaonongeka, munthu wamkati anali akukonzeka. Nkhondo zauzimu zimene Paulo amakuma nazo zotsatira zake zinali kukula mu uzimu. Chimene chinali chofunikira kwa iye si chimene chimaoneka ndi maso, koma zimene zimachitika mu dziko lauzimu.

Mmalo mosiya kumenya nkhondo, Paulo anaphunzira chipambano. Pa II Akorinto, iye akufotokozera kuti Mulungu:

- Anamulanditsa iye kale
- Akumulanditsa mu nyengo zatsopano
- Adzumulanditsa mu nyengo zamtsolo

CHIPAMBANO

Pasatengera kusautsika, mavuto, kuchita kakasi kumene Paulo anakumana nako, Iye anakwanitsabe kunena mau awa kumapeto kwake kwa moyo:

Ndalimbana nako kulimbana kwabwino, ndatsiriza njirayo, ndasunga cikhulupiro: (II Timoteo 4:7)

Ngati mwaphunzira kupambana pankhondo ngakhale mutangonja pakumenyana, mukhoza kukwanitsa kunenanso mau awa....” **NDALIMBANA NAKO KULIMBANA KWABWINO!**”

KUYENDERA PERETE

1. Lembani vesi Yotsogolera kucholera mu zolemba zankhondo.

2. Malinga ndi zitsanzo zimene zaperekedwa mu phunziro ili, tchulani zitsanzo zinayi za anthu amene anagonjetsedwa pakumenyana koma ndikupambana pa nkondo.

3. Tchulani njira zinayi zimene mungatsate kuti mupitilirebe kumenya nkondo ngakhale mutangonja pakumenyana

4. Tchulani vesi imene mukhoza kugwiritsa ntchito ngati Satana akutsutsana nanu pamene mwalephera.

5. Perekani vesi mu Baibulu imene imaonetsera kuti mukhoza kudzukanso ngakhale mutangonjetsedwa pakumenyana ndi Satana.

6. Kodi ndi chiani chimene Paulo anaphunzira pakugonja kwake ku Asiya?

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku limeneli)

MACHITACHITA ALUSO.

1. Kodi munayamba mwagonjetsedwapo ndi Satana pankhondo? Gwiritsani njira zimene zaperekedwa muphunziro limeneli kuti mugonjetse kulempha kwanu.

- Zindikirani kulempha kwanu.
- Lapani
- Konzaninso mphamvu zanu zauzimu.
- Bweleraninso kunkhondo.

2. **Njira imodzi imene Satana amagwirita tchito kuti agonjetse okhulupirira ndi chinyengo.**

Kunyenga ndi kumpangitsa munthu kuti akhulupirire zinthu zimene ndi zabodza kapena kuti kumusocheretsa munthu. Zina mwa zinthu zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza chinyengo ndi izi:

- Satana ndi wachinyengo ndipo iye samangonyenga anthu okha ayi ngakhalenso maiko (Chivumbulutso 20:10)
- Machitidwe a Satana ndi achinyengo komanso osalungama: II Atesalonika 2:20
- Timachenjezedwa kuti chinyengo chidzafalikira II Timoteyo 3: 13.
- Chifukwa chakuti chinyengo chidzachuluka, tiyenera kukhala osamala ndi zinthu zimene zimaonetsera kubweranso kwa Khristu Yesu Mateyu 24; Marko 13; II Atesalonika 2:3
- Tiyenera kusamala ndi iwo amene amagwiritsidwa ntchito ndi Satana kuti akanyenga anthu Akorinto 11:13; Tito 1:10; II Petro 2:13; II Yohane 7
- Wina aliyense osapulumsidwa amanyengeka ndi mtima wake: Yeremiya 17:9
- Wina aliyense osapulumsidwa amanyedwa ndi uchimo wake: II Akorinto 4:4; Ahebri 3:13
- Simukuyenera kuvomereza zoyankhula zonyenga zimene sizimagwiriza ndi mau a Mulungu. Aroma 16:18; I Akorinto 4: 2.

Mukhoza kunyengedwa ndi zinthu izi:

- Ngati mumvera nthano zachabe: Akolose 2:8.
- Ngati mudalira chuma ndi kulolera zilakolako za thupi Mateyu 13:22; Marko 4:19; Aefeso 4:22.
- Ngati muli akungomva chabe mau koma osawachita: Yakobo 1:22.
- Ngati munena kuti mulibe uchimo: I Yohane 1:8.
- Ngati mumvera anthu oipa II Timoteyo 3:13.
- Ngati mungatenge nokha kukhala opambana pamene musali choncho: Agalatiya 6:7.
- Ngati muganiza kuti simungakolore zimene mumafesa: Agalatiya 6:7
- Ngati mumaona kuti anthu osalunga adzalowa mu Ufumu wa Mulungu. I Akorinto 6:9.
- Ngati mungaone kuti ndinu a nzeru chifukwa choti muli ndi nzeru ya dziko lino: I Akorinto 3:18.

- Ngati mumaoneka kuti ndinu auzimu koma pamene lilime lunu losagonjetsedwa limaonetsa chikhalidwe chanu chenicheni. Yakobo 1:26.
- Ngati simukhulupilira kuti Yesu anabwera kuthupi II Yohane: 7.
- Ngati mumona ngati kuti simungachimwe kapena kuti tchimo silingakukhudzeni I Akorinto 15:33.

Mutawerenga mndandanda uli pamwambau, kodi pali zinthu zina zimene mukuona ngati mdani anakunyengani nazo? Ngati zili chomwechi, muyenera kuvomereza kuti munanyengedwa, ndi kulapa ndi kubwelera kunkhondo.

3. Baibulo limalengeza kuti Mulungu ndiye muomboro wathu pa nkhondi yauzimu. II Samuel 22:2; I Mbiri 11:14; Salimo 18:2; 40:17; 70:5; 144:2; Danieli 6:16.

- Amatilanditsa mmanja mwa adani athu: Oweruza 3:28.
- Yesu amatchedwa momboro Aroma 11:26.
- Simumalanditsidwa chifukwa cha mphamvu za munthu: Salimo 33:16
- Mulungu amapulumsa

Yobu wauphawi: Yobu 36:15

Onse amene awopa Iye: Masalimo 34:7

Angwiro: Miyambo 11:8,21

Onse oyenda mwanzeru: Miyambo 28:26

Oyera mtima: II Petro 2:9

- **Amatilanditsa ku:**

Anthu ankhanza: II Samueli 22:49

Adani athu: II Samueli 22:18; Masalimo 18:48; 78:42

Olimbana nafe: II Samueli 22:44; Masalimo 18:43

Mantha onse: Masalimo 34:4

Mantha a imfa: Ahebri 2:15

Mavuto athu: Masalimo 34:17; 54:7; 81:7

Nsautsi ndi chizuzi: Salimo 34:19; Machitidwe 7:10; II Timothy 3:11

Anthu olamura ndi oipa: Machitidwe 12:11

Chilamuro: Aroma 7:6

Kuchivundi: Aroma 8:21

Imfa yachiwiri: II Akorinto 1:10

Mphamvu yakumudima: Akolose 1:13

Mkwiyo umene ukudzao: I Atesalonika 1:10

Anthu ovuta: II Atesalonika 3:2

Nkhondo zanthu: Salimo 55:18

Imfa ya moyo wathu ndi kugwa: Salimo 56:13; 116:8

Onse odana nanu: Salimo 69:14

Gahena: Salimo 86:13

Nkhawa: Psalms 107:6

Chionongeko: Salimo 107:20.

MAU OMALIZA:

NKHONDO YAUZIMU YAIKULU YOMALIZA

Pali nkhondo imodzi yaikulu yomaliza imene idzathetse kumenyana kumene kwakhala kukuchitika kwa mibado ndi mibado. Satana ndi ankhondo ake adzagonjetsedwa ndipo Yesu Khristu adzalamulira kwa muyaya ngati mfumu ya mafumu.

CHAPUTALA 24

NKHONDO YOMALIZA

ZOLINGA

Pamapeto pamaphunziro awa muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza mwachidule zimene zidzachitike nkondo isanafike.
- Kufotokoza nkondo yomaliza.
- Kufotokoza mathero a Satana ndi mphamvu zoipa.

VESI YOTSOGOLERA

Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyedwa m'nyanja ya mota ndi sulfure, kumeneko kulonso ciromboco ndi mneneri wonyengayo; ndipo adzazunzidwa usana ndi usiku ku nthawi za nthawi. (Cibvumbulutso 20:10)

MAU OYAMBA

Monga mmene taonera kale muphunziro ili, chiweruzo cha Satana chinaperekedwa kale ndi imfa ndi chiukitso cha Yesu. Koma chiweruzochi chidzakwaniritsidwa pamene Yesu Khristu adzabwerenso kachiwiri.

Chaputala ichi chikhazikika pa nkondo yomaliza, nkondi imene idzangonjetse mpamvu zonse zoipa. Zotsatira za nkondo imeneyi kudzakhala kukhazikitsidwa kwa Ufumu wa Mulungu owoneka ndi maso, kulonga Yesu Khristu ngati mfumu ya mafumu ndi chiweruzo cha mphamvu zonse zokumidima.

ZOCHITIKA NKHONDO ISANAFIKE

Zina mwa zinthu zikuluzikulu zimene zidzachitike nkondo isanafike ndi izi:

KUBWERANSO KACHIWIRI KWA YESU

Baibulo limafotokoza kuti Yesu adzabweranso kudzatenga okhulupirira. Iye analonjeza kwa ophunzira ake nati:

... M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikudali kutero, ndikadakuuzani inu; pakuti ndipita kukukonzerani inu malo. Ndipo ngati ndipita kukakonzerani inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso. (Yohane 14:2-3)

kubweranso kwayesu kumatchedwa mkhwaturo. Zambiri zokhudza kubwerano kwa Yesu chifukwa cha okhulupirira ake kumafotokozeredwa pa I Atesalonika I Atesalonika 4: 13-18. Mavesi amenewa amaonetsa zinthu izi:

- Yesu mwini ndi adzabwera (Vesi 16)
- Kudzakhala chikukitso cha anthu okhulupirira amene ali mmanda (vesi 16)
- Kudzakhala mkwaturo. Mkwaturo ndi kutengedwa kwa munthu kuchoka malo ena ndi kupita malo ena. Anthu okhulupirira adzatengedwa ndi Yesu kuti akakumane naye. (werengani vesi 17)
- Okhulupirira amene anafa ndi amene adzakhale moyo adzayanjanitsidwa pamodzi ndi Khristu Yesu (Vesi 17)

Anthu ena amakhulupirira kuti mkwaturo udzachitika mazunzo asanafike ndipo kuti anthu onse okhulupirira sadzakumana ndi chizunzo chimenechi. Ena amakhulupirira kuti mkwaturo udzachitika pakatikati pa chizunzo. Pamene ena amati mkwaturo udzachitika pamapeto pa chizunzo. Koma mfundo imene anthu ambiri amakhulupirira ndi yakuti mkwaturo udzachitika chizunzo chisanafike. Maganizo osiyana amabwera chifukwa cha njira zosiyana za kamasulidwe Ka Baibulo. Koma chofunika kutsata ndi kuzindikira ndi chakuti muyenera kukhala okhulupirira weniweni wa Yesu. ndi okonzeka kutengedwa pamodzi ndi Yesu Khristu. Palibe munthu amene amadziwa nthawi yeniyeni imene izi zidzachitike:

Koma za tsiku ilo ndi nthawi yace sadziwa munthu ali yense, angakhale angelo a Kumwamba, kapena Mwana, koma Atate yekha. (Mateyu 24:36)

Ngakhale kuti palibe amene amadziwa nthawi yakubwera kwa Yesu Khristu, Yesu Khristu anapereka zizindiliro zimene zidzaonetsera kuti nthawi yayandikira. Mukhoza kuwerenga zambiri za izi pa Mateyu 24.

CHIZUNZO:

Baibulo limafotokoza za nthawi yowawitsa pa dziko lonse lapansi ya chizunzo. Iyi ndi nthawi imene mphamvu zakumidima zidzakhale zikugwira ntchito kwambiri mu mbiri yonse ya dziko lapansi. Satana adzakhazikitsa utatu wake onyansa wa iye mwini, aneneri onyenga ndi chilombo (Chivumbulutso 13; 16:13-14). kudzera mu choipa m'magome am'mwamba, adzachita zodabwitsa zambiri ndi kusocheretsa anthu ambiri. Iwo adzafuna kulambiridwa komaso adzaika chizindikiro chaumwina chapadera pa athu awo onse.

Malingana ndi Danieli (9:24-27), chizunzo chidzachitika kwa masiku okwana 126 kapena kwa miyezi yokwana makumi anayi ndi awiri. Pakhala nyengo zowawitsa zambiri padziko lapansi, koma iyi idzakhala nthawi yowawitsa kwambiri kusiyana ndi zowawa zina zimene anthu akhala akukumana nazo.

1. Izi zidzachitika dziko lonse lapansi osati malo amadzi okha ayi:

Popeza unasunga mau a cipiri canga, Inenso ndidzakusunga kukulanditsa mu nthawi ya kuyesedwa, ikudza pa dziko lonse lapansi, kudzayesa iwo akukhala padziko. (Cibvumbulutso 3:10)

2. Anthu adzazindikira kuti chimariziro cha nthawi chafika.

nanena kwa mapiri ndi matanthwe, Igwani pa ife, ndipo tibiseni ife ku nkhope ya iye amene akhala pa mpando wacifumu, ndi ku mkwiyo wa Mwanawankhosa; cifukwa lafika tsiku lalikuru la mkwiyo wao, ndipo akhoza kuima ndani? (Cibvumbulutso 6:16-17)

3. Kukula kwa chizunzo kudzakhala kwakulu kumene sikunaonekeponso.

Pali chiweruzo cha mulungu chosiyanasiyana chimene chidzagwe pa dziko lapansi munthawi yachizunzoyi. Chiweruzo chimenechi chikufotokozedwa pa Chivumbulutso 6,8,9 ndi 16 komanso mateyu 24:4-14. Mazunzo amenewa ndi chilango chifukwa cha tchimo lokana Mulungu.

ULAMULIRO WA YESU WA ZAKA CHIKWI (1000)

Ulamuloro umeneu ndi wa zaka 1000 ndipo udzachitika pamapeto pa chizunzo. Iyi ndi nthawi imene Yesu adzalumulira dziko lapansi ndi chilungamo chonse.

Ili ndi cimo la Aigupto, ndi cimo la amitundu onse osakwerako kusunga madyerero a misasa. (Zakariya 14:19)

Mzinda wa Yerusalemu udzakhala likulu la boma limeneli:

Ndipo padzakhala masiku otsiriza, kuti phiri la nyumba ya Yehova lidzakhazikika pa nsonga ya mapiri, ndipo lidzakwezedwa pamwamba pa zitunda; mitundu yonse idzasonkhana kumeneko. Ndipo anthu ambiri adzanka, nati, Tiyeni tikwere kunka ku phiri la Yehova, ku nyumba ya Mulungu wa Yakobo; ndipo Iye adzatiphunzitsa za njira zace, ndipo tidzayenda m'mayendedwe ace; cifukwa m'Ziyoni mudzaturuka cilamulo, ndi mau a Yehova kucokera m'Yerusalemu. (Yesaya 2:2-3)

Ulamuliro umeneu usanayambe, Satana, angero ndi ankhondo ake onse adzamangidwa.

Pamapeto pake padzachitika nkondo yaikulu kwambiri pa dziko lapansi:

Ndipo cinagwidwa ciromboco, ndi pamodzi naco mneneri wonyenga amene adacita zizindikilo pamaso pace, zimene anasokeretsa nazo iwo amene adalandira lemba la cirombo, ndi iwo akulambira fano lace; iwo awiri

**anaponyedwa ali moyo m'nyanja yamoto yakutentha ndi sulfure :
(Cibvumbulutso 19:20)**

Ndipo anagwira cinjoka, njoka yakaleyo, ndiye mdierekezi ndi Satana, nammanga iye zaka cikwi, namponya kuphomphe, natsekapo, nasindikizapo cizindikilo pamwamba pace, kuti asanyengenso amitundu kufikira kudzatha zaka cikwi; patsogolo pace ayenera kumasulidwa iye kanthawi. (Cibvumbulutso 20:2-3)

NKHONDO YOMALIZA

Pamapeto pa zaka chikwi chimodzi, padzakahala nkondo yaikulu ndi Satana:

Ndipo pamene zidzatha zaka cikwi, adzamasulidwa Satana m'ndende yace; nadzaturuka kudzasokeretsa amitundu ali mu ngondya zinai za dziko, Gogo, ndi Magogo, kudzawasonkhanitsa acite nkondo: ciwerengero cao ca iwo amene cikhala ngati mcenga wa kunyanja. Ndipo anakwera nafalikira m'dziko, nazinga tsasa la oyera mtima ndi mudzi wokonedwawo: ndipo unatsika mota wakumwamba nuwanyeketsa. Cibvumbulutso 20:7-9

Mulungu adzatumiza moto kuchokera kumwamba ndipo izi zidzagonjetsa adani ake onse.

Ndipo anakwera nafalikira m'dziko, nazinga tsasa la oyera mtima ndi mudzi wokonedwawo: ndipo unatsika mota wakumwamba nuwanyeketsa. (Cibvumbulutso 20:9)

Cholinga cha nkondi imeneyi ndi kugonjetsa Satana ndi kuti onse akavomereze kuti Yesu ndi ambuye wa onse. Ichi chidzakhala chimariziro cha chikonzero chonse cha Mulungu cha nthawi zonse:

Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko.

iyi ndi nkondo yauzimu imene yakhala ikumenyedwa chiyambireni kuukira kwa Satana kufikira mu mbiri ya dziko lapansi. (Aefeso 1:9-10)

MATHERO A SATANA

Mathero a utatu wa Satana mu nyanja ya moto:

Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyedwa m'nyanja ya mota ndi sulfure, kumeneko kulonso ciromboco ndi mneneri wonyengayo; ndipo adzazunzidwa usana ndi usiku ku nthawi za nthawi. (Cibvumbulutso 20:10)

Ziwanda zonse za Satana zidzaponyedwa mu nyanja ya moto:

**awiri adzakhala opera pamphero; mmodzi adzatengedwa, ndi wina adzasiyidwa.
(Mateyu 24:41)**

Ngakhale ziwanda zimene zimadziwirati mathero ake. Pamene Yesu anapita malo otchedwa Genesareti, Iye anakumana ndi athu awiri ogwidwa ndi ziwanda ndipo iwo anafuula kwa iye nati:

Pomwepo Iye adzanena kwa iwo a ku dzanja lamanzere, Cokani kwa Ine otembereredwa inu, ku mota wa nthawi zonse wokolezedwera mdierekezi ndi amithenga ace: (Mateyu 25:41)

Ndipo onani, anapfuula nati, Tiri nanu ciani, inu Mwana wa Mulungu? mwadza kuno kodi kutizunza ife, nthawi yace siinafike? (Mateyu 8:29)

CHIWERUZO

Zolengedwa zonse zidzaweruzidwa ndi Mulungu ndipo iyi imatchedwa nthawi yachiweruzo. Onse amene adzafe ali osakhulupirira adzaukitsidwa kuti aweruzidwe. Chufukwa chakuti sanakhulupilire ndikuvomereza Yesu Khristu ngati mpulumutsi, iwo adzaweruzidwa kumoto wamuyaya ku Gahena:

Ndipo ndinaona akufa, akuru ndi ang'ono alinkuima ku mpando wacifumu; ndipo mabuku anatssegulidwa; ndipo buku lina linatssegulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabuku, monga mwa nchito zao. Ndipo nyanja inapereka akufawo anali momwemo, ndipo imfa ndi Hade zinapereka akufawo anali m'menemo; ndipo anaweruzidwa yense monga mwa nchito zace, Ndipo imfa ndi Hade zinaponyedwa m'nyanja yamoto. Iyo ndiyo imfa yaciwiri, ndiyo nyanja yamoto. Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m'buku la moyo, anaponyedwa m'nyanja yamoto. (Cibvumbulutso 20:12-15)

Okhulupirira enieni amene analapa machimo awo adzakhala moyo wao onse ndi Mulungu kumwamba (Chivumbulutso 21)

Mkhondo yaikulu yauzimu idzakhala kuti yatha:

Ndipo anampatsa ulamuliro, ndi ulemerero, ndi ufumu, kuti anthu onse, ndi mitundu yonse ya anthu, ndi a manenedwe onse, amtumikire; ulamuliro wace ndi ulamuliro wosatha wosapitirira, ndi ufumu wace sudzaonongeka. (Danieli 7:14)

CHIGONJETSO MUDZIKO LAUZIMU

Chaputala ichi ndi chomaliza mu phunziro la nkondo yauzimu. Koma zoonza zake ndi zakuti palibe mathero akuphunzira phunziro limeneli. Mupitilirabe kuphunzira ukadaulo wina pamene mukhale mukumenya nkondo ngati mmene amachitira msirikali wakuthupi.

Pamene mukumaliza phunziro ili, tikufuna tikutsikimizireni kuti mukhoza kukhala ongetsa amphamvu zamdaniyo pankhondo ina iliyonse imene mukhale mukumenya. Koma muyenera kukumbuka kuti:

- Chigonjetso chanu pa nkhondo yauzimu chilipodi chifukwa sizimatengera inuyo koma Mulungu:

Mfumu imene ya ulemerero ndani? Yehova wamphamvu ndi wolimba, Yehova wolimba kunkhondo. (Masalmo 24:8)

- Ndinu otetezedwa ndi Mulungu pamene mukumenya nkhondo:

Yehova Ambuye, ndinu mphamvu ya cipulumutso canga, Munandiphimba mutu wanga tsiku lakulimbana nkhondo (Masalmo 140:7)

- Pamene mwafooka, Mulungu adzakutonhozani

Pakutinsu pakudza ife m'Makedoniya thupi lathu linalibe mpumulo, koma tinasautsidwa ife monsemo; kunjako zolimbana, m'katimo mantha. Koma iye amene atonhoza; (2 Akorinto 7:5-6)

- Mulungu adzakulimbikitsani pakati pa nkhondo:

Pakuti Ine Yehova Mulungu wako ndidzagwira dzanja lako lamanja, ndi kunena kwa iwe, Usaopo ndidzakuthandiza iwe. (Yesaya 41:13)

Ine, Inedi, ndine amene nditonhoza mtima wako; kodi iwe ndani, kuti uopa munthu amene adzafa, ndi mwana wa munthu amene adzakhala ngati udzu; (Yesaya 51:12)

- Palibe chida chosulidwa chimene chidzapambana:

Palibe cida cosulidwira iwe cidzapindula; (Yesaya 54:17)

- Chigonjetso chilipo pa dziko lonse lapansi:

Pakuti ciri conse cabadwa mwa Mulungu cililaka dziko lapansi; ndipo ici ndi cilako tililaka naco dziko lapansi, ndico cikhulupiriro cathu. (1 Yohane 5:4 5)

- Mutha kukhala ndi chigonjetso pa thupi:

Koma iwo a Kristu Yesu adapacika thupi, ndi zokhumba zace, ndi zilakolako zace. (Agalatiya 5:24)

- Chigonjetso chilipo pa Satana:

Ndipo Mulungu wa mtendere adzaphwanva: Satana pansu pa mapazi anu tsopano lino. (Aroma 16:20)

- Chigonjetso chikhoza kupezeka pa imfa ngakhale kumanda kumene.

Ndidzawaombola ku, mphamvu ya kumanda, ndidzawaombola kuimfa; imfa, miliri yako iri kuti? manda, cionongeko cako ciri kuti? Kulekerera kudzabisika pamaso panga. (Hoseya 13:14)

Mdani wotsiriza amene adzathedwa ndiye imfa. 21 Imfawe, cigonjetso cako ciri kuti? Imfawe, mbola yako iri kuti? (Akorinto 15:26,55)

Iye wameza imfa ku nthawi yonse; (Yesaya 25:8)

- Chigonjetso chilipo pa zonse zidzikweza mutsutsana ndi Mulungu:
Ndi kugwetsa matsutsano, ndi cokwezeka conse cimene cidzikweza pokana chidziwitso ca Mulungu, ndi kugonjetsa ganizo lonse ku kumvera kwa Kristu; (2 Akorinto 10:5)
- Chigonjetso chilipo pa mphamvu zonse za mdani:
Taonani, ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka ndi zinkhanira, ndi pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo; ndipo kulibe kanthu kadzakuipsani konse.... (Luka 10:19)
- Nthawi zonse kumbukira kuyamika Mulungu chifukwa chachigonjetso pa nkondo:
koma 23 ayamikike Mulungu, amene atipatsa ife cigonjetso mwa Ambuye wathu Yesu Kristu. (1 Akorinto 15:57)
- Pamene nkondo yatha, mudzakhala ogonjetsa:
Mwa ici mudzitengere zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoza kuima citsutsire pofika tsiku loipa, ndipo, mutacita zonse, mudzacirimika. (Aefeso 6:13)

KUYENDERA PERETE

1. Lembani vesi yotsogolera kuchokera muzolembe zankhondo.

2. Fotokozi zinthu zimene zidzachike nkondo yomaliza isanafike.

3. Fotokozerani za nkondo yomaliza. Kodi idzachitika liti? Ndipo chidzachitike ndi chiani kwa mdani ogonjetsedwayo?

4. Kodi mathero a Satana ndi mphamvu zakumidima ndi chiani?

(mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa Buku ili)

MACHITACHITA ALUSO

1. Satana amatchera msampha kwa anthu okhulupirira. Msampha ndi matchera amene cholinga chake ndi kukugwirani ukapolo. Muyenera kuunukira moyo wanu ngati simunakodwe pamsampha ndi zinthu izi:
 - Msampha wansodzi: Masalimo 91:3; 124:7
 - Anthu ochimwa: Masalimo 119:110
 - Milomo yanu: Miyambo 18:7
 - Abwenzi oipa: Miyambo 22:24-25
 - Mantha pa munthu: Miyambo 29:25
 - Satana: I Timoteyo 3:7; II Timoteyo 2:26
 - Chuma: I Timoteyo 6:9
 - Tchimo: Miyambo 29:6
 - Onyoza: Miyambo 29:8
 - Milungu yabodza: Ekisodo 23:33; Judges 2:3
 - Abwenzi ochimwa: I Samueli 18:21
 - Mapangano ndi anthu osakhulupirira: Ekisodo 34:12 Werengani mfundo zokhudza mipingo isanu ndi iwiri mu pa Chivumbulutso 2-3. Malinga ndi nkondo yauzimu, ndi madera ati amene anthu awa amalephera? Ndi malangizo ati amene Mzimu wa Mulungu anapereka ndi cholinga choti akonzeso njira zao.
2. Pakadali pano ndinu ngonjetsi! Kuchokera muphunziro limeneli mwaphunzira zinthu izi: Mukhoza kugonjetsa mphamvu ya oipayo 1 Yohane 2:13-14.
 - Yesu analigonjetsa dziko lapansi: Yohane: 16:4:4.
 - Chifukwa amakhala mwa inu, mukhoza kugonjetsa dziko: I Yohane 4:4
 - Munagonjetsa chifukwa chafukwa chakubadwanso mwatsopano komanso ndi chikhulupiriro chanu: I Yohane 5:4-5.
 - Munagonjetsa ndi mwazi wa Yesu komanso ndi umboni wapakamwa panu: Chivumbulutso 12:11.
3. Pali malonjezo okoma amene akuperekedwa kwa anthu ogonjetsa. Awa ndi anthu amene anagonjetsa mphamvu zauzimu zoipa pakumenya nkondo yonera yauzimu.
 - Adzadya chipatso chamtengo wamoyo: Chivumbulutso 2:7
 - Adzadya mana obisika: Chivumbulutso 2:17
 - Adzavekedwa chovala choyera: Chivumbulutso 3:5
 - Adzakhala nsanamira ya mkachisi wa ambuye Chivumbulutso 3:12
 - Adzakhala pamodzi ndi Yesu pamando wake wachifumu: Chivumbulutso 3:21
 - Adzakhala ndi dzina latsopano: Chivumbulutso 2:17
 - Adzakhala ndi ulamuliro pamaiko onse: Chivumbulutso 2:26
 - Dzina la Mulungu lidzalembedwa pa iwo: Chivumbulutso 3:12
 - Adzakhala ndi ubale wapadera ndi Mulungu: Chivumbulutso 21:7
 - Adzakhala ndi nthanda ya m'mwawa (Yesu): Chivumbulutso 2:28
 - Adzachitiridwa umboni ndi Yesu pamaso apa Atate: Chivumbulutso 3:5
 - Sadzakhudzidwa ndi imfa yachiwiri: Chivumbulutso 2:11

-Mayina awo sadzachotsedwa mu buku la moyo: Chivumbulutso 3:5

-zonze zidzakhala zao: Chivumbulutso 21:

4. Ili ndi phunziro lanu lomaliza muphunziro la nkondo yauzimu, koma zoonza zake ndi zakuti mukhala mukuphunzirabe zinthu zina zokhudza phunziro limeneli. Mukhalabe mukumenya nkondo zauzimu kufikira nthawi imene mudzaitanidwe ndi ambuye. Pamene mukhale mukumenya nkondo, mukhala mukuphunzira zambiri kudzera mu chipambano chanu angakhale kugonjetsedwa kumene. Muyenera kuyamba kulemba nkondo zimene mudzidutsamo, kaya ndi chipambano kapena chigonjetso, lembani zimenezi. Koma chimene muyenera kudziwa ndi chakuti kugonjetsedwa ndi chinthu chakanthawi kochepe chabe. Nkhani yaikulu ndi yakuti muyera kubweleranso kukamenya nkondo. Mukhoza kugonja pakumenyana, koma tili nacho chitsimikizo chochokera kwa Mbuye wathu wamakamu kuti chipambano chotsiriza chili mbali yathu!

ZINA ZA PADERA

NKHONDO ZIKULUZIKULU ZA M’BAIBULO

Paulo Mtumwi anakambako za kufunika kwa Chipangano Chakale. Anati:

Koma izi zinacitika kwa iwowa monga zoticenjeza, ndipo zinalembedwa kuticenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya pansi pano adafika pa ife. (1 Akorinto 10:11).

Chipangano Chakale chimaperekeka chitsanzo chakuti ife tiphunzirepo. Mukawerenga Chipangano Chakale, mupeza kuti muli nkondo zambiri zimene zinamenyedwa kuthupi ndithu. Mwina nkumadabwa kuti chifukwa nkhani zimenezi zikupezeka m’Baibulo. Kufunika kwa nkondozi kukuposera kungodziwa m’mene zinakhalira. Njira zomenyera nkondo za m’Chipangano Chakale kuthupi zitha kugwiritsidwa ntchito pa nkondo yauzimu pogonjetsa mdani.

Chigawo choonjezerachi chikusanthula nkondo za m’Chipangano Chakale pofuna kutengera njira za nkondo yawo nkuzigwiritsa ntchito mu nkondo yauzimu. Msilikari wa kudziko amawerenga njira za magulu ena a nkondo omwe adachitapo bwino kuti aphunzire luso lapamwamba. Inunso mutha kukuza luso lanu la nkondo yauzimu poona momwe anzathu a m’Baibulo anachitira.

NKHONDO YOFUNIKIRA

“Nkhondo yofunikira” ndi nkondo yaikulu imene imamenyedwa kuti zidziwike wamphamvu ndi ndani. Ndi nkondo yomenyedwa nthawi zovuta kwambiri. Imathera nkupita chitsogolo kapena kubwerera, kupambana kapena kugonja. Imakhala kuti wina wapalamula (kutenga dera) kapena wina akuziteteza (kuteteza dera). Mu njira ina, ndi kulimbana kofunika kwambiri. Chigawo choonjezera chino chikukamba za “nkondo zofunikira” za mu Chipangano Chakale. Njira zimene zinagwiritsidwa ntchito zitha kukuthandizani pomenya “nkondo zofunika” zanu muuzimu.

CHIFUKWA CHA NKHONDO ZA M’CHIPANGANO CHAKALE

Nkhondo m’Chipangano Chakale zimamenyedwa pa zifukwa zauzimu zotsatirazi:

1. Anthu a Mulungu agonjetse mphamvu zoipa zimene zikanatha kuwaika mu ukapolo.
2. Kutu anthu a Mulungu alande dera lomwe Mulungu wawapatsa kuchokera m’manja mwa adani.
3. Kulanga anthu a Mulungu akachimwa pamaso pa Mulungu.

Nkhondo zathu zauzimu zimachitika pa zifukwa zomwezi.

MFUNDO ZIKULUZIKULU

Musanayambe kusanthula nkondo iliyonse payokha payokha, nkofunika kuti muyambe mwamvetsa mfundo za nkondo m’Chipangano Chakale popeza zimayendera limodzi ndi zauzimu.

MFUNDO 1

Nkhondo imene Mulungu amakhala kuti waivomereza ndipo, iye amalonjeza chitetezo kwa ziphona za nkhoodoyo. Deut. 20:1-4.

MFUNDO 2

Adani a Israel amakhalanso adani a Mulungu. Anthu amayenera kudalira Mulungu osati okha kuti apambane (Oweruza 5:31; Eksodo 17:16). Akatero Mulungu amawamenyera nkhoodo.

MFUNDO 3.

Likasa linali chizindikiro chakuti Mulungu ali pakati pawo pamene akumenya nkhoodo (Eksodo 30:6; 25:21-22). Likasa limakhala patsogolo patsogolo pa gulu lankhoodo la Israel kutsimikizira kupezeka kwa Mulungu (1 Samuel 4:1-11). Mu Chipangano Chatsopano, Yesu ndi Mzimu Woyera mkati mwa okhulupirira ndi chitsimiko cha kupezeka kwa Mulungu pawo (Yohane 14:16-17).

MFUNDO 4

Ana a Israel amayenera kukhala oyera kuti Mulungu awamenyere nkhoodo (Deuteronomu 23:9-14). Amayenera kudzipatula ku chirichonse cha uchimo.

MFUNDO 5

Onse amantha samaloledwa kupita ku nkhoodo (Deut. 20:8; Oweruza 7:1-6). Anthu amantha amathawa nkhoodo iri mkati.

MFUNDO 6

Anthu otanganidwa ndi zochitika m'moyo samaloledwa kupita ku nkhoodo. Deuteronomu 20:5-8 akunena kuti munthu wongokwatira kumene samapita ku nkhoodo kwa chaka chimodzi. Izi zinabo chomwecho chifukwa amalabadira kwambiri za mkazi wake, kumanga nyumba, ndi kukhazikika. Amakhala wotangidwa ndi zinthu ngati zimenezi chotero sakanatha kukhala wa mphamvu ku nkhoodo. Paulo akuchenjeza Timoteyo kuti, “Msilikari satanganidwa ndi ntchito wamba” (2 Timoteyo 2:4). Yesu anachenjezanso za kukhala wotanganidwa ndi zinthu za dziko lapansi. Mu uneneri wa Daniel, timamva kuti wokana Khristu “adzafooketsa oyera mtima” ndi zotangidwitsa za moyo uno.

MFUNDO 7.

Anthu a Mulungu amayenera kumenya nkhoodo kufikira mdani ataonongedwa kwatunthu (Numeri 31:10-11).

MFUNDO 8.

Malinga ozungulira Israel anali ofunikira kwambiri pa chitetezo chawo. Malinga amakhala mikono khumi mu litali (10m high) ndi mikono itatu mu mjintcho (3m wide). Alonda amaikidwa pamwamba malinga kulondera mzinda kwa adani. Chipangano Chatsopano chimayerekeza wokhulupirira ndi “mzinda womangidwa pa tanthwe.” Monga mwaphunzira kale, muli ndi malinga okutetezani ku ziwembu za mdani.

MFUNDO 9.

Nkhondo iriyonse imatsegulidwa ndi lipenga la mkulu wa nkhondo (Oweruza 7:18) ndipo, ikatha, lipenga limalira kuitana asilikari kuti achoke ku nkhond (2 Samuel 2:28; 18:16). Yesu anaomba lipenga lauzimu m'mene anatilamulira kuti timuke ku dziko lapansi ndi Uthenga Wabwino natipatsa ulamuliro pa mdani (Mateyu 28:18-20). Tsiku lina lipenga lidzalira kutiitana kuti tikapume kumenya nkhondo (1 Atesalonika 4:16-18).

DONGOSOLO LA PHUNZIRO LINO

Nkhondo iriyonse yomwe yakambidwa m'chigawo chino ikuphatikizapo:

- Vesi: Werengani nkhanu ya nkhondo iriyonse m'Baibulo lanu.
- Bwalo lomenyera nkhondo: Malo eni eni komwe kunachitikira nkhondo.
- Mphamvu zomwe zikulimbana: Zindikirani magulu omwe akulimbana m'nkhondoyo.
- Chifukwa cha nkhondoyo: Chifukwa chomenyera nkhondo.
- Njira: Njira zogonjetsera kapena zifukwa zolepherera nkhondo. Njira zina m'Baibulo zikumabwerezedwa. Mwachitsanzo, anthu akhala akuuzidwa mobwereza bwereza kuti asaope mdani. Ngati njira imeneyo yatchulidwa kale kamodzi, njira imeneyo siibwerezedwanso m'phunziro lino.

NKHONDO ZIKULUZIKULU ZA M'BAIBULO

Ndime: Genesesi 14.

Malo a nkhondo: Dani, pafupi ndi Mtsinje wa Yorodani.

Mphamvu zolimbana: Abraham ndi mafumu anayi a kum'mawa.

Chifukwa cha nkhondo: Adani agwira Loti m'bale wake wa Abrahamu.

Dongosolo la nkhondo:

1. Mukalowa m'dera la adani yembekezerani nkhondo nthawi ina iriyonse.
2. Abrahamu anaika asilikari ake m'magulu awiri osavuta kuwayang'anira. Timagulu tochepati tinagonjetsa asilikari a mafumu anayi. Chigonjetso sichitengera kuchuluka kwa asilikari omwe alipo, koma dongosolo, kukonzekera ndi kagwiridwe ka ntchito.

Ndime: Eksodo 14-15

Komenyera nkhondo: M'mbali mwa Nyanja Yofiira malire ndi Aigupto.

Mphamvu zolimbana: Israel ndi Aigupto

Chifukwa cha nkhondo: Israel amathawa ku ukapolo wa kwa Aigupto. Anali akuthawa Aigupto pamene anapanikizika ndi Nyanja Yofiira kutsogolo kwawo Aigupto kumbuyo kwawo.

Dongosolo la nkhondo:

1. Musayang'ane nyengoyo: "Israel anatumukula maso" naona Aigupto akuwalondola (Eksodo 14:10-11). Atayang'ana nyengo yao osati Mulungu, anachita mantha.
2. Osayang'ana m'mbuyo: Aisrael anayamba kuganzira za zinthu zabwino za ku Aigupto, chomwe ndi chizindikiro cha ukapolo wa uchimo (Eksodo 14:12). Mukamayang'ana m'mbuyo simungapite chitsogolo muuzimu.
3. Musaope: Uthenga woyamba wa Mulungu kwa Israel unali wakuti, "usaope" (Eksodo 14:13). Mantha amalefula pamaso pa mdani. Chikhulupiriro chimakulimbikitsani kuti muchitepo kanthu.
4. Khalani chete: (Eksodo 14:13). Muzikhala chete nthawi zonse pokha pokha Mulungu akuuzeni chochita. Osathawa chifukwa cha mantha.
5. Muloleni Mulungu akumenyerani nkhondo. Nkhondo siyanu. Simukuyenera kuyamba kusala kudya. Mulungu akumenyerani nkhondo (Eksodo 14:14).
6. Upezeni mtima: Mulalole mdani akuopsezeni mpaka kutaya mtima (Eksodo 14:14).
7. Pitani chitsogolo, osabwerera: Mulungu anauza Israel kuti aponde madzi nawoloke. Madzi anali odzadza koma samayenera kubwerera koma kulowa m'madzi osefukirawo (Eksodo 14:15-16, 21).
8. Tsimikizikani kuti Mulungu achita zozizwa: (Eksodo 14:19-31). Mukatsatira njira zauzimu za nkhondo yauzimu, Mulungu achita zozizwa ndi kukumenyerani nkhondo kugonjetsa mdani. Muona Mulungu akuchita zodabwitsa pomenyera nkhondo anthu ake.

Ndime: Eksodo 17:8-16

Malo omenyera nkhondo: Onani Deuteronomu 25:17-18. Amaleki anathira nkhondo Israel kumbuyo, koma analibe mphamvu.

Njira zomwenyera nkhondo:

1. Gonjetsani ndi pemphero: Israel sakanatha kupambana ndi lupanga lokha. Zomwe Mose anachita zimatengedwa ngati pemphero (Eksodo 17:9-11). Zimaonetsa mtima wodalira kwatunthu pa Mulungu zomwe zidabweretsa chipambano (Eksodo 17:11).
2. Gwirani "ndodo ya Mulungu": Mose anagwiritsa ndodo ya Mulungu, ngati chizindikiro cha ulamuliro wauzimu. Mukalowa mu nkhondo gwiritsani ulamuliro wanu wauzimu. Dziwani chomwe muli mwa Khristu ndi ulamuliro womwe muli nawo.
3. Mverani utsogoleri wauzimu: Yoswa anachita molingana ndi momwe Mose adamuuzira. (9-10). Mulungu waika atsogoleri pakati pathu. Amagwiritsa ntchito iwowa kupereka malangizo kuti zolinga zake zikwaniritsidwe. Ngati wina aliyense angafune kukhala mtsogoleri chisokonezo chimayambika.
4. Pitani kukamenya nkhondo: Si nkhondo zonse zomenya moteteza dera lathu ayi. Nthawi zina mukuyenera kumenya nkhondo yopamalamula ndipo kuti mukhale wamakani (9).
5. Funani thandizo: Mulungu amatha kudzutsa anthu akuti akuthandizeni kulimbana ndi nkhondo zanu zauzimu. Mulungu anaitana Yoswa kuti akhale mtsogoleri wa nkhondo ndipo kuti Mose anali mtsogoleri wauzimu. Aroni ndi Huri anathandiza Mose kumgwira manja pamene analema.

6. Kumbukirani zigonjetso za m'mbuyo: Kukumbukira zigonjetso zimene zakhalapo m'mbuyomu zimapereka mphamvu zina kuti mulimbe mtima pakukumana ndi mdani. Mulungu anauza Mose kuti alembe nkhani ya nkondo iyi m'bukhu la chikumbukiro ndipo azimkumbutsa Yoswa nthawi zonse (14). Yoswa yemwe anaikidwa kukhala wolowa m'malo mwa Mose, anatsogoloera ana Israel kugonjetsa Dziko la Malonjezano.

Ndime: Numeri 14.

Malo omenyera nkondo: Dziko la mapiri la Homa.

Mphamvu zolimbana: Israel kulimbana ndi Amaleki Akenani.

Chifukwa cha nkondo: Israel anapita kukachotsa Amaleki ndi Akenani kuti atenge dziko.

Dongosolo la nkondo:

1. Osadula: Israel anadandaula ataona nyengo yawo (2-3). Kudandaula ndi kunyinyirika sikumkondweretsa Mulungu (11).
2. Musagalukire pamaso pa Ambuye. Kuukira ndi tchimo. Mukuyenera kusiiiratu kuukira (9).
3. Musamale ndi malipoti abodza: Satana amasokeretsa kudzera mu zinthu zabodza komanso kupangitsa gulu kulankhula zinthu zimene sizoonza kuti aputsitse anthu ena. Si nthawi zonse pamene gulu limakhala kuti likunena zoonza (36-38).
4. Mverani liu la Mulungu: Mulungu ananena momveka bwino kuti abwerere kunka ku chipululu koma iwo anapita dera lina losiyana (25)
5. Musakhale ndi kulimbika mtima kodutsa mulingo: Israel anangolowa mu nkondo mopanda dalitso la Mulungu (42-44). Kupezeka kwa Mulungu ndi kofunika pa nkondo yauzimu.
6. Pangani ziganizo mwa chikhulupiriro, osati mwa mantha. Ziganizo zopanga mwa mantha zimathera nkugonjetsedwa.

Ndime: Numeri: 21:1-3

Malo a nkondo: Homa.

Mphamvu zolimbana: Israel ndi Aradi Mkenani, mfumu ya mtundu.

Chifukwa cha nkondo: Israel anakakamizidwa kulowa mu nkondo iyi. Silinali dongosolo lawo kuti alowere kum'mwera.

Njira zomenyera nkondo:

1. Zindikirani kuti kulephera ndi mau a kanthawi. Nkondo yolimbana ndi Mfumu Arad ndi Akenani inamenyedwa m'dera limene inalephereka zaka 38 zapitazo (Numeri 14:45). Ngakhale Israel adalephera poyambapo, koma mu nthawi iyi anapambana. Kulephera kusatengedwe ngati nkwa muyaya. Mudzakhala wolephera mukadzasiya kuyesera.

2. Phunzirani kuchokera nkulephera kwanu kwa kale: Mulungu atha kugwiritsa ntchito kulephera kwanu kwa kale kuti akuphunzitseni zinthu zina zauzimu. Israel anaphunzira kuti akuyenera kukhala ndi Mulungu nthawi zonse ku nkhondo (2-3). Mufunsi Mulungu zomwe akufuna kukuphunzitsani kudzera nkulephera kwanu.

Ndime: Numeri 21:21-32

Malo a nkhondo: Yahaz

Magulu omenyana: Israel ndi Aamori

Chifukwa cha nkhondo: Mose amafuna kulanda dziko lolonjezedwa ndi Mulungu kuzambwe kwa Yordani. Anapempha kuti adutse mwa mtendere (vs. 21-22), koma Siho, mfumu ya Aamori, adakana (23).

Dongosolo la nkhondo:

1. Dziwani kuti simungazembe kumenyana nkhondo. Ngati mukufuna kulandira lonjezano la Mulungu, nkhondo ndi yosapeweka. Mdani sangalole mudutse mulandire dalitso lanu mwa mtendere.

Ndime: Numeri 31

Malo a nkhondo: Zigwa za Moab

Magulu olimbana: Aisraeli ndi Amidian

Chifukwa cha nkhondo: Mulungu analamulira kuti Amidiani aonongedwe onse popeza anali anthu oipa opembedza Baal (Numeri 25).

Dongosolo la nkhondo:

1. Dziyeretseni nokha: Mulungu anakhazikitsa njira yodziyeretsera kuti Aisraeli ayitsatire asanapite ku nkhondo. Mulungu anangokhazikitsa njirayo, iwowo amayenera ayitsatire. Ngati mukufuna kuti Mulungu akumenyereni nkhondo, mukuyenera kukhala woyeretsedwa muuzimu. Wakhazikitsa njira kudzera mwa Khristu Yesu, komano inuyo mukuyenera kuchitapo kanthu.
2. Musatanganidwe ndi zofuna zanu: (25-54). Ku nkhondo munthu sayenera kutanganidwa ndi zinthu zina kuti pakhale chigonjetso cha nonse.

Ndime: Deuteronomu 2:24-37

Malo a nkhondo: Yahaz

Magulu olimbana: Israel ndi Siho, m'Amori, mfumu ya Hesbon.

Chifukwa cha nkhondo: Siho adakana kulola Aisrael kuti aoloke mwa mtendere kunka kutsidya kwa Mtsinje wa Yordani kunka ku dziko limene Mulungu adawapatsa.

Dongosolo la nkhondo:

1. Tengani chimene Mulungu wakupatsani: Mulungu anali atawapatsa kale Aisrael dziko la la malonjezano la Kenani lomwe ndi chithunzithunzi cha moyo wodzala ndi Mzimu (24). Wakumpatsaninso inu cholowa. Ndi chanu kale, kudikira kuti muchitenge. (Onaninso nkhondo ya Endrei mu Numeri 21:33-35. Dongosolo lomweli lotenga chimene Mulungu wakupatsani likuonekeranso mu nkhondo iyi).
2. Musiyeni Mulungu akumenyereni nkhondo: Siho anathira nkhondo yoopsa Aisrael koma anagonjetsedwa popeza Mulungu anamenyera nkhondo ana ake (31, 33).
3. Dziwani kuti palibe chomulaka Ambuye: Mu Kenani munalibe mzinda ngakhale umodzi womwe unali wa mphamvu kwambiri koti Mulungu sakanatha kuonjetsa (36). Palibe malimba ena alionse m'moyo wanu omwe sangathe kugonjetsedwa.

Ndime: Deuteronomu 3:1-11

Magulu olimbana: Israel ndi Ogi mAmori, mfumu ya Bashan.

Chifukwa chomenyera nkhondo: Og, chiphonacho, anaopseza azondi pamene anapita kukayendera dziko (13:33), anabwera ndi asilikari ake kuti athire nkhondo Aisrael.

Dongosolo la nkhondo:

1. Tsimikizikani kuti Mulungu adzapereka adani anu mdzanja lanu: Lamulo la Mulungu kwa Israel kuti athire nkhondo Ogi linatsana ndi lonjezo lakuti Iye wapereka Ogi mdzanja lawo (3).
2. Gonjetsani zothodwetsa zonse: Msinkhu wa malinga a mizinda ya mdani komanso kuopsa kwa mfumu yawo sikunagonjetsa asilikari a Yehova. Kwa iwo amene apatsidwa mphamvu ndi Ambuye, palibe chingawalake.
3. Lengezani zipatso za chigonjetso: Deuteronomu: 3:8-11 akulankhula momveka bwino za chipatso cha nkhondo ya Israel ku Endrei. Nkhondo iriyonse mungamenye imakupatsani mwayi wakuti mupeze “chipatso china cha chigonjetso” m'moyo wanu wauzimu.

Ndime: Yoswa 6

Malo a nkhondo: Yeriko

Magulu olimbana: Aisrael ndi mfumu ya Yeriko pamodzi ndi anyamata ake oopsa.

Chifukwa chomenyera nkhondo: Mulungu anauza Yoswa kuti atsogolere Aisrael pa kugonjetsa mzinda wa Yeriko.

Dongosolo la nkhondo:

1. Zindikirani kuti njira za Mulungu, si njira zanu: Posatengera kuti nyengoyo ikuoneka yophweka motani, mukuyenera kudalira Ambuye. Njira zake ndi malingiliro ake ndi osiyana ndi anu (Yesaya 55:8). Mulungu amagwiritsa ntchito chimene dziko lachipeputsa kuti akagonjetse amphamvu (1 Akorinto 1:27). Nthawi zina amalowerera mu nyengo za ana mu njira zooneka zopusa ku dziko lapansi. Israel anadalira Mulungu pomenya nkhondo posatengera kuti ikuoneka yophweka motani. (Onani 1 Akorinto 1:25).
2. Pemphani chitsimikizo chakuti Mulungu ali nanu: Likasa la Yehova latchulidwa kasanu ndi kanayi mu 6-13 ndipo likuimilira kupezeka kwa Mulungu pakati pa anthu ake. Musanalowe mu nkhondo iriyonse, onenesetsani kuti Mulungu ali nanu.
3. Gwiritsani njira ya chete: Israel anauzidwa kuti azungulire mwa kachetechete (kupatula kuopa malipenga) kufikira atauzidwa kuti afuule (vs. 10). Njira ya kachetechete igwiritsidwe ntchito pa nkhondo kufikira mutalandira ulamuliro kuchokera kwa Mulungu za zomwe mulankhule ndi nthawi yoti mulankhule.

Ndime: Yoshua 7

Malo a nkhondo: Mzinda wa Ai.

Mbali zolimbana: Aisraeli ndi Aamori

Chifukwa cha kulimbana: Yoshua amapitilirabe kutsogolera Israel kutenga dziko la malonjezano.

Dongosolo la nkhondo:

1. Musaphwanye malangizo a Mulungu: Kukondera kwa Mulungu kunachoka pa Israel chifukwa cha tchimo la Akani zomwe zinapangitsa kuti Israel akanthidwe kwakukuru (vs. 1-5). Tchimo limazembera chigonjetso.
2. Musamuonere pansu mdani: azondi anadelera chiwerengero cha Ai (2-4). Musaonere pansu mphamvu ya mdani ya kupha, kuba ndi kuononga. Komanso kuona zinthu ndi maso a thupi kumabweretsa mantha. Muli ndi mphamvu pa mphamvu zonse za mdani.
3. Pezani ndi kuthana ndi tsinde la kugonjetsedwa kwanu: Pakakhala kugonjetsedwa ndiye kuti pali chifukwa. Israel anathana ndi tchimo molingana ndi momwe Mulungu ananenera (13, 25, 26). Zimenezi zinabwezeretsa kukonderedwa kwa Mulungu pa Israel. Kutu kupezeka kwa Mulungu kukhalebe pa inu, mukuyenera kuthana ndi tchimo mwa kuvomereza ndi kulapa.
4. Pewani zilakolako za thupi: Tchimo la Akani linali lppitirira – anaona, anasilira ndipo anatenga (21). Mu 1 Petro 2:11 timauzidwa kuti “tipewe zilakolako za thupi, zomwe zimalimbana ndi moyo.” Chilakolako cha maso si cha Atate, koma cha dziko lapansi (1 Yohane 2:16). Kuchokera pamene Satana anayamba kulimbana ndi munthu woyamba, zilakolako zathupi zakhala zothandizira kugonjetsedwa (Genesesi 3).

Ndime: Yoswa 8.

Malo a nkondo: Ai

Mbali zolimbana: Israel ndi amuna a mu Ai

Chifukwa cha kulimbana: Mulungu analamulira Israel kuti atenge Ai ndipo kuti mu nthawi iyi apambana.

Dongosolo la nkondo:

1. Thandizanani wina ndi mnzake: Israel anagwira ntchito limodzi kugonjetsa mdani. Mlaliki 4:9-12 amanena kuti taonjezera mphamvu zolimbana ndi mdani tikagwira ntchito mothanizana wina ndi mnzake.
2. Khalani okonzeka: Yoswa anauza gulu la nkondo kuti likhale lokonzeka (vs. 4). Inu muli pa nkondo yauzimu. Mukuyenera kukhala wokonzeka nthawi zonse kulimbana ndi mdani.
3. Gwiritsani ntchito lupanga: Lupanga la Yoswa linakhala chizindikiro chokodelera amuna obisala m'tchire (18-19). Okhulupirira ali ndi lupanga lauzimu ndilo Mau a Mulungu (Aefeso 6:17). Gwiritsani ntchito lupangali kuchenjeza ena za chiwembu cha mdani.
4. Tembenukani ndi kukumana ndi mdani wanu: Aisraeli omwe anathawira m'tchire anatembenukira adani awo kuwathamangitsa ndi kuwakantha (21). Tembenukirani ndi kukantha mdani wanu mu mphamvu za Ambuye. "Dzichepetseni pamaso pa Mulungu, mkanizeni woipayo, ndipo adzakuthawani" (Yakobo 4:7).
5. Yang'anani pa Mulungu osati pa chigonjetso: Yoswa anatsogolera anthu mkupembedza atatha kugonjetsa (vs. 29-31). Nthawi zina timakokomezeka chigonjetso chatu ndi momwe tachitira. Koma Mau a Mulungu amatichenjeza kuti "Iye amene ali chiriri adziyang'anire kuti angagwe" (1 Akorinto 10:12).

Ndime: 10:1-27

Malo a nkondo: Gibeon

Mbali zolimbana: Israel ndi mafumu asanu Aamori ku Yerusalemu, Hebron, Jarimu, Lakisi ndi Eglon ndi asilikari awo.

Chifukwa cha kulimbana: Yoswa anapemphedwa kukathandiza a Gebion popeza mfumu ya Yerusalemu inakonza zokawathira nkondo chifukwa chopanga mgwirizano ndi Israel. Mafumu asanuwa anafunitsitsa kuletsa Israel kuti asatenge dziko limene Mulungu analonjeza.

Dongosolo la nkondo:

1. Ikani mdani pansu pa mapazi anu: Kuika mapazi anu pa khosi, chizindikiro chakale cha kugonjetsa, kukuchitika ndi mkulu wa kagulu ka nkondo ka Yoswa (vs. 24-25). Yesu anati Iye ndi mutu wa thupi lake, Mpingo. Waika mphamvu zonse za mdani pansu pa mapazi ake. Ngati ndife thupi lake ndiye kuti mapazi athu ali pa khosi la mdani.
2. Khalani wamphamvu ndi wolimbika mtima: Awa ndi Mau a Mulungu kwa inu mnthawi ya kulimbana kwakukuru. Mphamvu zanu zimachokera nkudziwa kuti Mulungu ali mbali

yanu. Kutsimikizika uku kumakupatsani mphamvu ndi kulimbika mtima mkati mwa kulimbana ndi mdani (25).

Ndime: Yoswa 10:28-43

Malo a nkondo: Kumwera kwa Palestina

Magulu olimbana: Israel ndi mizinda ya Kumwera kwa Palestina

Chifukwa cha nkondo: Yoswa anayambitsa nkondoyi pofuna kulanda dera la Kumwera kwa Palestina.

Dongosolo la nkondo:

1. Thirani nkondo madera ofunikira: Nkondo ya Yoswa inali ngati ziphaliwali ku mizinda yofunikira ya Kenani kuti aononge okhala mzindawo (28-43). Mukathira nkondo malimba ofunikira a mdani m'moyo wanu (monga thupi) mumachepetsa kuthekera kwa mdani kukuthirani nkondo.

Ndime: Yoswa 11

Malo a nkondo: Ku madzi a Meron

Magulu olimbana: Israel ndi mafumu a kumpoto kwa Kenani pansu pa utsogoleri wa Yabin, Mfumu ya Hazori.

Chifukwa cha nkondo: Kutsatira malamulo a Mulungu, pamene Yoswa amatsogolera Aisrael kulanda dera lina la dziko la Kenani.

Dongosolo la nkondo:

1. Pilirani: Yoswa anamenyana nkondo ndi mafumu a dzikoli kwa zaka zisanu ndi chimodzi (18). Kupilira (kukhala wokhulupirika mu nkondo) ndi kofunika pogonjetsa malimba, kuthamangitsa okhalamo (moyo wa uchimo) ndi kutenga zonse zomwe Mulungu walonjeza.
2. Musaope kukula kwa mphamvu za mdani (vs. 4).

Ndime: Oweruza 6:1-8:35

Malo a nkondo: Chigwa cha Yezirilu

Magulu olimbana: Gideon ndi amuna 300 molimbana ndi Amidian ndi Amaleki.

Chifukwa cha nkondo: Popeza Israel anachimwa, Mulungu anawapereka mdzanja la Amidian kuwachita ukapolo kwa zaka zisanu ndi ziwiri. Pamene Israel analapa nalira kwa Mulungu, Iye anatomiza Gideon kukawamasula.

Dongosolo la nkondo:

1. Kumvera chenjezo...Chimo limaika mu ukapolo: Israel anakhala wopanda mphamvu pamaso pa adani ake chifukwa cha tchimo (1-5). Tchimo limabweretsa ukapolo wauzimu wa Satana.
2. Kubwezeretsedwa kumachokera kwa Mulungu: Kuzunzika kwa Israel ndi Amidian kunampangitsa kubwera mogonja pamaso pa Mulungu kupempha mamasulidwe (6-8). Pamene mwatengedwa ukapolo kudzera mu uchimo wanu, chiyembekezo chokhacho chimene muli nacho ndi Mulungu kuti akumasuleni.
3. Pezani malo anokha ndi Mulungu: Gideon anali yekha pamene Mulungu amamuitana kukapulumsa Israel (11-14). Atsogoleri auzimu amphamvu akuyenera kumapeza nthawi yokhala wokha ndi Mulungu. Ngati mungathandize anthu ena kudzera mu utumiki wa mamasulidwe, njira iyi ndiyofunika kwambiri.
4. Gwetsani maguwa a mafano: Gidion anagwetsa ndi kuononga maguwa a Baal (25-31). Mukuyenera kugwetsa malimba a mdani ndi kuononga mafano onse omwe akutsamwitsa kudzipereka kwanu kwa Mulungu.
5. Kutidwani ndi Mzimu wa Mulungu: Mzimu wa Mulungu unatsika pa Gidion kumpatsa mphamvu kuti akakwaniritse cholinga cha Mulungu (34). Mukamakutidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera pa zifukwa zomwezi (Machitidwe 1:8).
6. Funafunani mulingo wozama wa chikhulupiriro: Gidion anafuna chikopa kuti akhulupirire Mulungu (36-40). Okhulupirira ena sangakhulupirire Mulungu pokhapokha ataona chizindikiro cha kuthupi. Mukuyenera kukhala ndi chikhulupiriro chozama chokhazikika pa Mau a Mulungu ngakhale zinthu zooneka ndi maso zikutsutsa zimene mukukhulupirirazo. Onani Machitidwe 27:20-25.
7. Musadzidalire nokha: Mulungu anachepetsa chiwerengero cha asilikari kuti Aisrael angadzitamandire. Mulungu amagwira ntchito m'moyo wanu kuchotsa kudzidalira nokha kuti mukazindikire mfundo yakuti chigonjetso chimachokera kwa Yehova.
8. Musakaikere: Ngakhale Mulungu anatsimikizira, Gidion anakaikirabe za kukumana ndi mdani. Anali woti sanatsogolerepo gulu la nkondo chiyambireni ndipo anthu ake anali opanda maphunziro ndi luso la nkondo (7:9, 10). Nthawi zina mumakaika kuchita chinthu chachilendo chimene Mulungu wakuuzani. Mutha kumadzimva kuperewera pa luso la ntchitoyo. Musakaikere. Mulungu amapatsa kuthekera iwo amene wawaitana.
9. Lunjikani mantha a mdani: Mulungu analola Gidion kuti amve zoopseza za Amidian. Mukamva zochititsa mantha, mumatulukira kufooka kwanu. Yakobo 2:19 amanena kuti ziwanda zimakhulupirira Mulungu ndipo zimanthunthumira ndi mantha. Lunjikani mantha a mdierikezi ndi mphamvu ya Mulungu.

Ndime: Oweruza 15

Malo a nkondo: Lehi.

Magulu olimbana: Samson ndi Afilisti

Chifukwa cha nkhondo: Samson anathira nkhondo Afilisti chifukwa cha nkhani ya pabanja. Afilisti amalozza chala mkazi wake chifukwa cha zomwe Samson anachita ndipo anabwezera powaononga ndi moto. Kubwezeranaku kunapirirabe pakati pa Samson ndi Afilisti.

Dongosolo la nkhondo:

1. Dziwani kuti Mulungu amatembenuza kugonjetsedwa kukhala chigonjetso: Pamene adani a Samson anafuula ndi chimwemwe pa kugonjetsa kwao, Mzimu wa Mulungu unatsika pa Samson ndipo anadula zingwe zommanga m’manja (14). Anatenga fupa la bulu, nakantha adani ake ndikupha amuna chikwi. Chomwe chimaonenga ngati ndi kulephera chinasanduka kukhala chipambano kwa chiphona cha Israel (15). Palibe kugonjetsedwa ndi mdani komwe Mulungu sangakusithe kukhala chigonjetso.
2. Mtengeni Mulungu kukhala thandizo lanu: Itatha ntchito yopha amuna chikwi a Afilisti, Samson anamva ludzu. Izi zinapangitsa moyo wake kukhala pa chiopsezo kuti Afilisti ena angabwere kwa iye nkubwezera kuphedwa kwa anthu awo. Nkusautsika kwake, iye anaitanira pa Ambuye (18). Mulungu amatipatsa mphamvu ku nkhondo komanso ndiye thandizo lathu.
3. Imwani pa kasupe wa Ambuye: Poyankha kulira kwake, Mulungu anapangitsa madzi atumphuke pa nthaka. Samson anamwa napezanso mphamvu (19). Yesu anati, “Ngati wina amva ludzu, abwere kwa ine, namwe” (Yohane 7:37). Asilikari a dziko amafuna nthawi yopuma ndi kumwa madzi, ifenso timafuna kuthetsa ludzu ndi kupezanso mphamvu zina. Ena amachita izi kudzera m’zisangalalo, zotsangalatsa ndi zokonda. Koma kupeza mphamvu zina kweni kweni kumachitika pa “kasupe wa Ambuye.”

Ndime: Oweruza 20

Malo a nkhondo: Gibeya

Magulu olimbana: Abenjamini ndi Aisraeli ena.

Chifukwa cha nkhondo: Mdzakazi wa m’Levi anagwiridwa ndi kuphedwa ndi gulu la amuna a ku Gibeya. M’Levi anaitana akuluakulu a mafuko onse kuti amve nkhanayi ndi kupeza chochita. Onse anagwirizana kulanga amuna a Gibeya kupatula Abenjamini omwe anaima kuteteza a Gibeya.

Dongosolo la nkhondo:

1. Funsani uphungu wa Mulungu: Israel anapita pamaso pa Mulungu mobwerezabwereza kupempha nzeru pa dongosolo la nkhondo (18, 23, 26, ndi 28).
2. Khalani omvana ndi amnzanu: Mitundu ina ya Israel inapempha mtundu wa Benjamini kuti upereke adaniwo mdzanja lawo kuti awalange. Israel amafunisitsa kuchotsa choipacho polanga anthu opalamulawo (13). Ngati wokhulupirira tikuyenera timvane ndi Mulungu pochotsa tchimo m’moyo wathu popereka madera amenewa kwa Iye.
3. Osaleka kumenya nkhondo: Nkhondo ziwiri zoyambilira Aisrael anakanthidwa ndi asilikari a Benjamini. Aisrael analira, kusala, ndi kupitanso kwa Ambuye kukapeza

uphungu. Anawauza kuti apirize kumenya nkondo ndipo awapatsa chipambano (vs. 18-28).

Ndime: 1 Samuel 4

Malo omenyera nkondo: pakati pa Afeki ndi Ebenenza

Magulu olimbana: Aisrael ndi Afilisti

Chifukwa cha nkondo: Israel anamenyana ndi Afilisti, adani a Mulungu.

Dongosolo la nkondo:

1. Osadalira “zizindikiro” za Mulungu: Likasa la Yehova linakhala chizindikiro cha kupezeka kwa Mulungu pakati pa Israel anthu ake (4). Koma anthu samayenera kuika maso awo pa likasa koma kuyang’ana Mulungu wa Likasalo.

Ndime: 1 Samuel 11.

Malo a nkondo: Bezek

Magulu olimbana: Nahashi m’Amori ndi amuna a Yabesi pamodzi ndi Saulo m’Israel.

Chifukwa cha nkondo: Aamoni anathira nkondo mzinda wa Israel Yabesi-Giliadi. Sauli anasonkhanitsa asilikari nawagonjetsa (11).

Dongosolo la nkondo:

1. Konzekerani nkondo m’mamawa: Sauli anathira nkondo Aamoni m’mapanda kucha (11). Bwerani kwa Mulungu m’maola a m’mapanda kucha kuti “mubvale zida za Mulungu” (Aefeso 6:11-17).

Ndime: 1 Samuel 13-14

Malo a nkondo: Mikimash

Magulu olimbana: Aisrael ndi Afilisti

Zifukwa za nkondo: Yonatani anapha msilikari wa Afilisti ku Geba.

Dongosolo la nkondo:

1. Khalani wodekha mu nyengo ya zovuta: Kusadekha kwa Sauli kunapangitsa Sauli kutaya mwai wokhala mtsogoleri (13). Anali wa mantha pona asilikari ake akuthawa pamaso pa Afilisti. Anakanika kumvera lamulo la Mulungu lakuti adikire. Mu nyengo yazovuta, musalole kuti mantha akukakamizeni kuchita zinthu zopusa.

2. Tsindikani kudzipereka osati kuchiwerengero cha asilikari: Israel anapambana pa nkondo zake chifukwa cha amuna odzipereka osati chifukwa cha gulu lalikuru. (14:6).

Ndime: 1 Samuel 17.

Malo a nkondo: Chigwa cha Ela.

Magulu olimbana: Israel (Davide) ndi Afilisti (Goliati).

Chifukwa cha nkondo: Gulu la nkondo la Afilisti linasonkhana kuti likathire nkondo Israeli. Gulu la nkondo la Israel linaima mbali ina ya chigwa kuteteza. Chiphona cha Afilisti, Goliati, anagamula kuti nkondo ichitike pakati pa iye ndi chiphona chimodzi cha Israel.

Dongosolo la nkondo:

1. Pezani mphamvu mu zigonjetso zam'mbuyo: Davide anaona chigonjetso pa kupulumutsa nkosa zake ku nyama zolusa za mtchire. Anatsimikizira mfumu Sauli kuti iye ateteza nkosa za Mulungu (vs. 24-36). Chikhulupiriro chomwe chaumbika ndi zokoma zam'mbuyo chimakonzereketsedwa ku zokhoma za mtsogolo.
2. Onani zovuta ngati mwayi wa Mulungu: Nyengo iriyonse yovuta imapereka mwayi wakuti Mulungu aonetsere mphamvu zake kwa anthu kudzera mwa inu. Davide anaona Goliati ngati mwayi wakuti Israel aone mphamvu ya Mulungu osati ngati nyengo yoopseza (vs. 25, 45-47).
3. Gwiritsani ntchito zida zovomerezeka: Davide anakana zida za dziko za Sauli popeza anali asanagwiritsepo ntchito ku nkondo (vs. 38, 39). Nkondo zauzimu sizimenedwa ndi dongosolo ndi zida za dziko lapansi. Zikuyenera kumenyedwa ndi njira zovomerezeka zauzimu.
4. Kumanani ndi mdani mdzina la Ambuye: Goliati anabwera ndi lupanga, nthungo ndi zina koma Davide anakumana ndi mdani mdzina la Ambuye (45-47).
5. Kumbukirani kuti nkondoyi ndi ya Yehova: Mdani atha kumaoneka ngati ali ndi mphamvu zoposa, koma nkondo ikakhala ya Yehova chigonjetso chimakhala chosakaikitsa. Davide anatsimikizira kuti chigonjetso chimabwera ndi Mulungu osati munthu. "Si mphamvu, si nkondo koma Mzimu wa Ambuye, atero Yehova wa Makamu" (Zakariya 4:6).
6. Musangoyang'ana kuthekera kwanu kokha: Goliati anaona Davide ngati kamwana ka nthete komwe sikanamenyeko nkondo (33). Mulungu sationa ife monga m'mene tiliri, opanda kuthekera. Amationa chimene tingakhale ngati tingalole mphamvu yake ichite zazikulu mwa ife.
7. Lankhulani za chigonjetso: Davide anaona zomwe Mulungu wachita kale pa iye ndipo analankhula molimba mtima za chigonjetso cha Mulungu pa Goliati.
8. Zindikirani za cholinga cha nkondo yauzimu: Davide analankhula mu vesi 46... "Kuti dziko lonse likadziwe kuti kuli Mulungu."

Ndime: 1 Samuel 30

Malo a nkondo: Pafupi ndi Ziglag

Mbali zolimbana: Israel ndi Amaleki

Chifukwa cha nkondo: Pamene Davide ndi ankondo ake anali kutali ndi Ziglag (komwe amakhala mu nthawi iyi) adani anathira nkondo naotcha mudzi wawo komanso kulanda azikazi awo.

Dongosolo la nkondo:

1. Musalole kukhala kakasi: Amuna a Davide anali okwiya ndipo anaganiza zomuponya miyala (6), koma Davide anadzilimbikitsa yekha mwa Yehova. Mnyengo ya kukhumudwitsidwa kwakukuru pamene mukuima nokha, dzilimbikitseni nokha mwa Yehova. Musalole kukhala wosowa mtengo wogwira.
2. Lengezani kubwezeretsedwa kwa zonse zimene mdani watenga: Mdani amabwera kuti adzabe, kupha, ndi kuononga (vs. 1). Mulungu anauza Davide kuti alondole adani ndi kulanda zonse zimene mdani anatenga (vs. 8, 18).
3. Zindikirani kuti chigonjetso cha munthu m' modzi ndi chigonjetso cha onse: Vesi 24 ikupereka mfundo yofunikira kwambiri pa nkondo yauzimu. Iwo amene akugwira ntchito komanso amene “akudikira zinthu” akuyenera kugawana zinthu mofanana pa chigonjetso.

Ndime: 2 Samuel 5:1-16).

Malo a nkondo: Yerusalemu

Magulu olimbana: Aisrael ndi Ayebusi.

Chifukwa cha nkondo: Ayebusi anaona Yerusalemu ngati mzinda wamphamvu ndipo sungalandidwe. Davide analanda mzindawo naupanga kukhala likuru la Israel.

Dongosolo la nkondo:

1. Musalole kuyang'aniridwa pansu ndi chitonzo cha mdani: Ayebusi ananyoza Davide natama mzinda wao kuti sungalandidwe ndi “akhungu ndi olumala” (6). Davide sanalole kuti achepesedwe ndi chitonzo ichi (7). Pamene mdani akukutonzani nakupangani kudzimva kuperewera, lengezani Yohane 8:44.

Ndime: 2 Samuel 5:17-25

Malo a nkondo: Chigwa cha Refaimu.

Magulu olimbana: Aisrael ndi Afilisti.

Chifukwa cha nkhondo: Pamene Afilisti anamva kuti Davide wadzodzedwa kukhala mfumu ya Israel, anakonza chiwembu kuti alimbane naye.

Dongosolo la nkhondo:

1. Palamulani nkhondo: Davide sanadikire kuti adani adzamuyambe. Ananyamuka kukawapalamula. Musadikire mdani kuti adzakuyambeni.

Ndime: 2 Samuel 10

Malo a nkhondo: Dera la Helamu

Magulu olimbana: Aisraeli ndi Aamoni ndi Asuri

Chifukwa cha nkhondo: Mfumu ya Amoni inamwalira. Davide anatumiza anyamata ake kukatonthoza mwana wake ndi kumtsimikizira kuti ali naye limodzi. Koma mfumu yatsopanoyi inamvera uphungu wolakwika ndi kuuzidwa zinthu zambiri zabodza. Ananyoza Aisraeli mmalo molandira ulemu wawo. Anawameta ndevu mbali imodzi, nawang'ambira zovala zawo ndikuwabweza mwa manyazi (1-5).

Dongosolo la nkhondo:

1. Khalani a mtima umodzi pa nkhondo: Mkulu wa nkhondo wa Davide atazindikira kuti akuthiridwa nkhondo kuchokera mbali ziwiri, anagawa gulu lake pawiri. Ngakhale anagawidwa pawiri koma anagwira ntchito ndi mtima umodzi kufikira kugonjetsa adani awo. Tikhoza kukhala osiyana mitundu, zikhalidwe, kapena mipingo koma tili okhulupirira. Tikuyenera kugwirana manja ndikulimbana ndi mdani wathu pamodzi osati tokhatokha.

Ndime: 2 Samuel 21:15-22

Malo a nkhondo: Gobu ndi Gati

Magulu olimbana: Aisrael ndi Afilisti.

Chifukwa cha nkhondo: Afilisti anapitirira kulimbana ndi Aisrael. Iyi ndi nkhani ina ya kupitirira kwa nkhondo yawo.

1. Gonjetsani ziphona mdziko: Ziphona zambiri za Afilisti zinaphedwa mu nkhondo zimenezi. Ziphona izi zinazunza Aisrael kwa zaka zaka. Kodi pali ziphona za thupi zakalekale zomwe zikukuzunzani? Pitirizani nkhondo kufikira ziphona zonse zitagonjetsedwa.
2. Zindikirani kuti Mulungu amagwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana: Davide anagonjetsa Goliati mwa mphamvu za Ambuye ndi mwala chabe. Koma mu nthawi iyi akugwiritsa ntchito njira ina pogonjetsa ziphona (16-17). Musamuikire Mulungu poganiza kuti m'mene anachitira dzulo ndi momwe achitirensa lero.

3. Limbikitsani atsogoleri: Ngakhale atsogoleri atha kukhala ofooka mu nkondo, musawanene koma alimbikitseni ndi kuwathandiza.

Ndime: 1 Mafumu 20

Malo a nkondo: Samaria kenako ku Afeki.

Magulu olimbana: Ahab mfumu ya Israel ndi Benhadad mfumu ya Asuri.

Chifukwa cha nkondo: Benhadad, mfumu ya Asuri, inasonkhanitsa asilikari ake ndi kumema mafumu 32 kuti akathire nkondo Samaria.

Dongosolo la nkondo:

1. Zindikirani kuti mdani adzabwera: Mneneri wa Mulungu anauza mfumu ya Israel kuti adzikonzekeretse popeza mfumu ya Asuri idzabweranso kumthira nkondo (vs. 22). Ngakhale mutapambana motani, koma musatase popeza nkondo idakalipo. Mdani adzadzitoleranso mphamvu nadzuka kulimbana ndi anthu a Mulungu.
2. Musanamizidwe ndi mau okoma: Chifukwa cha kupusitsidwa kuti mfumu ya Asuri yagonjera ku Israel, Ahab anavomera kumlola Benhadad kuti amuke mu mtendere. Benhadad anali wodzikonda zomwe ndi zosemphana ndi Mau a Mulungu. Onani Miyambo 16:8.
3. Ikani zinthu zofunika poyambirira: Ahab anali ndi chikhumbokhumbo cholandanso madera ake. Mau akuti “ndipo pamene anyamata anu anali kupita apa ndi apo, ananyamuka” (vs. 40) akuonetsera kuti sanayike zinthu bwino m’ malo. Chifuniro cha Mulungu chimafunika kuika zinthu zofunika poyambirira.
4. Musamnyengelere mdani: Ahab anali nako kuthekera kothetsa nkondo pakati pa Israel ndi Asuri pothana ndi Benhadad. Koma atangommasula, nkondo inapitilira ndi zotsatira zoopsa (42).

Ndime: 2 Mafumu 3

Malo a nkondo: Moab

Magulu olimbana: Israel ndi abwenzu ake, Yuda ndi Edom, kulimbana ndi Amoabu.

Chifukwa cha nkondo: Moabu anaukira nakana kupereka msonkho ku Israel. Yehoram anapempha mfumu ya Yuda kuti imamthandize kulimbana ndi Moabu. Atangoiyamba nkondo, mfumu Edom inapita kukawathandiza.

Dongosolo la nkondo:

1. Yamikani Mulungu pa bvumbulutso: Elisa anayimbidwa nyimbo kuti alandire Mau kuchokera kwa Ambuye. Akadali chiyimbire woyimbayo, Mzimu wa Ambuye unatsika pa Elisa ndi mau a bvumbulutso (vs. 11-15). Mayamiko ndi njira ya mphamvu kwambiri

ku nkondo yauzimu. Mayamiko amakonzekeretsa mzimu wanu kuti ulandire mau kuchokera kwa Mulungu.

2. Konzekerani chipambano: Nthawi zina simungalandire chipambano chifukwa chifukwa chosakonzekera. Kunali chilala ndipo asilikari a Israel anali pafupi kufa chifukwa cha ludzu. Elisa anapempherera chozizwa. Mulungu anati, “Pangani ngalande m’chigwa chonse ichi.” Mulungu anadza ngalandezo ndi madzi (16-17). Mukuyenera kukonzekera kuti mukhale zotengeramo za madzi opereka moyo a Mulungu. Nthawi zina zimafika pofuna kuchotsedwa kwa “dothi” lauzimu m’moyo wanu.

Ndime: 2 Mafumu 6:8-23

Malo a nkondo: Dotani ndi Samaria

Magulu olimbana: Israel ndi Asuri

Chifukwa cha nkondo: Pamene Asuri analimbana ndi Israel, Elisa anabvumbulutsa malo opezeka gulu la nkondo la Asuri. Mfumu ya Asuri itazindikira kuti Elisa akubvumbulutsa malo obisala asilikari ake, anatumiza gulu la nkondo kuti likamgwire.

Dongosolo la nkondo:

1. Pempherani. Monga mwaonera kale, pemphero linali mbali imodzi ya nkondo za m’Chipangano Chakale. Mu nkondo iyi, Elisa anapemphera kuti Mulungu akanthe asilikari a Asuri ndi khungu (vs. 18). Pemphero ndi chimodzi mwa zida zoopsa kwambiri pa nkondo yauzimu.
2. Khalani ndi maso auzimu: Elisa anali ndi maso auzimu ndipo anakwanitsa kunena kuti: “Usachite mantha, popeza iwo akukhala ndi ife ali ambiri kuposa akutizungulira (Asuri)” (vs. 16).
3. Lolani mphamvu ya Mulungu ionekere: Pamene Aasuri anakhala akhungu, Elisa anawapititsa kwa mfumu ya Israeli ndipo anamuuzza kuti asaphe koma awatumize kwao kuti mphamvu ya Mulungu ionekere (18-23).

Ndime: 2 Mafumu 6:24-7:20

Malo a nkondo: Samaria

Magulu olimbana: Asuri ndi Israel

Chifukwa cha nkondo: Benhadad ndi gulu lake la nkondo linazungulira Samaria ndipo njala yoopsa inagwa mu mzindamo. Chakudya chinali chosowa komanso chokwera mtengo, kotero kuti anthu anali kudya zinyalala ndipo ena anadya ana awo eni.

Dongosolo la nkondo:

1. Pitanibe ngakhale zikuoneka zosatekha: Pamene akhate khumi anali kulingalira chochita pa vuto lawo, anadziwa kuti Aasuri akawapha. Ngati sachitapo kanthu afabe. Anaganiza

zochita zinthu zooneka zosatheka ndi zoopsa. Ananyamuka kupita ku mahema a Aasuri ndipo Mulungu apangitsa phokoso la mapazi awo kumveka monga ngati phokoso la gulu lalikuru la nkhondo ndipo anathawa, nasiya katundu wao (7:3-7). Munthu ukayamba kuchita chinthu chooneka chosatheka Mulungu amalowererapo.

2. Gawanani ndi okhulupirira ena: Akhate aja anagawirako anzawo za nkhani yabwinoyi. Muli ndi udindo wogawirako ena pa zazikulu zimene Mulungu wakuchitirani. Umboni wanuwo ulimbikitsa okhulupirira ena.
3. Musakaikire za mphamvu yoopsa ya Mulungu: Munthu wina sanalandire nawo dalitso la Mulungu chifukwa cha kukaikira mphamvu ya Mulungu (7:2, 17-20).

Ndime: 2 Mafumu 17

Malo omenyera nkhondo: Samaria

Magulu olimbana: Israel ndi Asiriya

Chifukwa cha nkhondo: Hosheya, mfumu ya Israel, amayenera kumapereka msonkho chaka ndi chaka kwa mfumu ya Asiriya. Israel analeka kupereka msonkhowo ndipo Asiriya anaganiza zomthira nkhondo:

Dongosolo la nkhondo:

1. Kupembedza ndi mfungulo ya mphamvu mu nkhondo yauzimu: Israel analeka kupembedza ndipo Mulungu anawapereka mdzanja la Asiriya (onani Yobu 1 ndi 2). Mukakanika kupembedza Mulungu, posachedwapa mukhala kapolo wa mdani.

Ndime: 2 Mafumu 19

Malo a nkhondo: Yerusalemu

Magulu olimbana: Asiriya ndi Israel

Chifukwa cha nkhondo: Hezekiya, mfumu ya Israel, inadalira Mulungu ndipo anafunisitsa kuononga mafano. Poonetsa kuti dziko lake likhale pa mtendere anapereka msonkho kwa mfumu ya Asiriya. Kenako analandira kalata yoopseza.

Dongosolo la nkhondo:

1. Musachite mantha ndi zooseza za mdani: Hezekiya anatenga kalata ya chiopsezo kupita nayo pamaso pa Mulungu. Mulungu anamuuza kuti asaope, popeza mdani adzachotsedwa mdzikolo. Monga m'mene Mulungu anagonjetsera Aasiriya, Iye wagonjetsanso Satana. Musamaope ziopsezo zake.

Ndime: 2 Mafumu 24:1-25:30

Malo a nkondo: Yerusalemu.

Magulu olimbana: Yuda ndi Babulo.

Chifukwa cha nkondo: Yuda anachitabe choipa pamaso pa Mulungu. Mapeto ake Mulungu analola kuti anthu atengedwe kunka ku ukapolo ku Babulo omwe anali ndi mphamvu kwambiri pa dziko lonse. Yerusalemu anaotchedwa ndipo malinga anagwetsedwa.

Dongosolo la nkondo:

1. Dziwani kuti tchimo limamlowetsa munthu mu ukapolo: Anthu a Mulungu anatengedwa ukapolo chifukwa chopitilirabe kukhala m'moyo wa tchimo osafuna kulapa. M'malo mogwiritsidwa ntchito kuti agonjetse mdani, anatengedwa ukapolo ndi adani awo.

Ndime: 1 Mbiri 14:8-17

Malo a nkondo: Chigwa cha Refaimu ndi Baal-perazim

Magulu olimbana: Israel ndi Afilisti.

Chifukwa cha nkondo: Pamene Davide anakhala mfumu ya Israel yense, iye anali chiopsezo chachikulu kwa Afilisti. Anakonza chiwembu chakumthira nkondo.

Dongosolo la nkondo:

1. Dikiranibe nkondo yofunikira kwambiri: Davide ndi asilikari ake anapambana nkondo yoyamba, koma siinali yofunikira kwambiri popeza sanalande madera onse (9-13). Mu nkondo yachiwiri, Mulungu anawapatsa chigonjetso chachikulu. Anathamangitsa Afilisti onse mdera la Israel (13-17).
2. Dikirani nthawi yoyenerera: Kudikira nthawi yabwino nkofunikira pomenya nkondo. Davide anadikira kuti Mulungu amtsogolere monga momwe analonjezera (14-16). Anthu amagonjetsa kapena kugonjetsedwa chifukwa chozindikira kapena kukanika kuzindikira nthawi yabwino.

Ndime: 2 Mbiri 12

Malo a nkondo: Yerusalemu

Magulu olimbana: Igupto ndi abwenzu ake kulimbana ndi Rehoboam mfumu ya Yuda.

Chifukwa cha nkondo: Rehoboam anali wosakhulupirika kwa Mulungu natsata njira zachitayiko za Akenani. Kuthiridwa nkondo ndi Shishak, mfumu ya Igupto, kunavomerezeka ngati chilango chochokera kwa Mulungu.

Dongosolo la nkondo:

1. Konzekerani muuzimu; Kukhala wokonzeka muuzimu ndi kofunika pa chigonjetso: Rehoboam anachita choipa chifukwa “sanakonzekeretse mtima wake pamaso pa Mulungu (14). Konzekeretsani mtima wanu pofunafuna Ambuye musanalowe mu nkondo yauzimu.
2. Dzichepetseni nokha: Pamene Rehoboam anadzichepetsa yekha, “Mulungu anampatsa kachigonjetso.” Sanalole kuti aonongeke kotheratu (5-7).
3. Gonjerani ku ntchito ya Mulungu: Ngakhale Mulungu amakhululuka, kusamvera kuli ndi zotsatira zake (vs. 8). Kugonjera kwa Mulungu ndi kwambiri poyerekeza ndi zimene dziko lapansi limafuna ife titachita. Onani Mateyu 11: 28:30.

Ndime: 2 Mbiri 18

Malo a nkondo: Ramoti-giliadi

Magulu olimbana: Aasuri ndi Ahab mfumu ya Israel komanso Yehosafati mfumu ya Yuda.

Chifukwa cha nkondo: Yehosafati anachita mgwirizano ndi Ahab nathira nkondo Aasuri.

Dongosolo la nkondo:

1. Musachite maubale osayenera: Patatha zaka 65 Israel ndi Yuda ali pa udani, Yehosafati anachita ubwenzi ndi Ahab. Ndipo mwana wake wa mwamuna anakwatira mwana wamkazi wa Ahab. Ubale uyu unabweretsa mavuto ambiri kwa Yehosafati komanso Yuda yense chifukwa cha chikunja choopsa chimene chinalowa mu Yuda. Maubale oipa sadzabala zipatso zabwino zauzimu.
2. Gwiritsani ntchito nzeru polandira uphungu: Asanapite ku nkondo, Ahab anaitana aneneri kuti amuuze mau ochokera kwa Yehova. Koma aneneri aganyu awa amangolankhula zokhazo zomwe Ahab amafuna kumva. Yehosafati anakakamira kuti Ahab ayitane aneneri amene salandira thandizo kuchokera kwa mfumu. Ahab anaitana Mikaya amene uneneri wake umachokera kwa Mulungu (1-16). Pofunika kukhala maso polandira uphungu wauzimu. Gulu likagwirizana pa china chake sindiye kuti agwirizanazo ndi chifuniro cha Mulungu.

Ndime: 2 Mbiri 20

Malo a nkondo: Chigwa cha Beraka.

Magulu olimbana: Amuna a Moabu, Amoni, ndi Phiri la Seri kulimbana ndi Yehosafati, mfumu ya Yuda.

Chifukwa cha nkondo: Maiko angapo anachita upo wofuna kulimbana ndi Yuda.

Dongosolo la nkondo:

1. Gwiritsani ntchito njira ya kusala kudya: Yehosafati analengeza kusala kudya mu Yuda yense (vs. 3). Mulungu amachita nanu molingana ndi ubale womwe muli nawo ndi Iye.

Kusala kudya sikusinthu Mulungu, kumasintha inuyo. Kumasintha ubale wanu ndi Mulungu zomwe zimakhuzanso yankho lake kwa inu. Onaninso Yona 3.

2. Ikani maso anu pa Ambuye: Yehosafati anapemphera, “Sitikudziwa choti tichite, koma maso athu ali pa inu” (vs. 15). Ngati pali chinthu chomwe amene angachikwanitse ndi Mulungu yekha, mpatseni mpata osati muziyesera panokha.
3. Kondwerani mkatikati mwa nkhondo: Panali gulu limene linaikidwa kuti liziyimba patsogolo pa gulu la nkhondo. Mulungu anawasokoneza adani ndipo anagonjetsedwa.

Ndime: 2 Mbiri 25:5-16

Malo a nkhondo: Chigwa cha mchere

Magulu olimbana: Edom ndi Amaziya mfumu ya Yuda.

Chifukwa cha nkhondo: Amaziya analimbana ndi mtundu wachikunja wa Edom.

Dongosolo la nkhondo:

1. Tsatirani ulangizi wa Umulungu: Pofuna kupanga asilikari ake kuti akhale amphamvu, Amaziya anabwereka zida kuchokera ku Israel. Chinthu ichi sichinankondweretse Ambuye ndipo analankhula mwa mneneri wake kuti Israel abwerere ndikuti ngati satero Amaziya agonjetsedwa. Amaziya anatsatira uphungu wa Umulungu uwu ndipo anapambana.
2. Wonongani mafano onse: Amaziya anayamba kupembedza mafano a ku Edom (14). Nkhondo yamphamvu yauzimu idzaononga mafano onse m’ moyo wanu, kaya ndi a mwala, kapena a mtengo, ngakhale a chuma.

Ndime: 2 Mafumu 25:17-24

Malo a nkhondo: Betisemes wa Yuda

Magulu olimbana: Yehoasi, mfumu ya Israel kulimbana ndi Amaziya mfumu ya Yuda.

Chifukwa cha nkhondo: Kudzitama pa chigonjetso cha ku Edom kunampangitsa Amaziya kukathira nkhondo Israel.

Dongosolo la nkhondo:

1. Kudzitama kumadzetsa kugonjetsedwa: Amaziya anadzadzidwa ndi matama chifukwa cha chipambano chakale. Izi zinamtsogolera kufuna kulimbana ndi Israel (17-19). Onani Miyambo 16:5.

Ndime: 2 Mbiri 28

Malo a nkhondo: Yerusalemu

Magulu olimbana: Yuda anathiridwa nkhondo ndi magulu a nkhondo a Aasuri, Israel, Edom, Filisti ndi Asiriya.

Dongosolo la nkhondo:

1. Zinthu zoipa za dziko lapansi zimabweretsa bwinja lauzimu: Ahaz anapembedza milungu yachilendo poganiza kuti zimumpatsa mphamvu za nkhondo. M'malo mwake, anatha (vs. 23). Zinthu zoipa za dziko lapansi zimayambitsa kusokonekera kwa moyo wauzimu.
2. Ngakhale amuna amphamvu amagwa ngati achoka pamaso pa Mulungu: Onani vesi 6.

Ndime: 2 Mbiri 32:1-23; ndi 2 Mafumu 19

Malo a nkhondo: Yerusalemu.

Magulu olimbana: Senakaribu, mfumu ya Asiriya ndi Hezekiah, mfumu ya Yuda.

Chifukwa cha nkhondo: Mfumu ya Asiriya inathira nkhondo Yuda ndi kuzungulira mizinda yotetezedwa.

Dongosolo la nkhondo:

1. Dulani njira zopezera zinthu za mdani: Hezekiya anadula njira ya Asiriya yopezera madzi ndi kumanganso malinga a mzinda (3, 5). Kugawikana mthupi la Khristu ndi njira imodzi imene mdierekezi amaidalira. Timampatsa mdierekezi mphamvu ngati tilimbana tokhatokha ngati okhulupirira kudzera mlilime. M'malo molimbana ndi okhulupirira amnzathu, tiyeni tiwamangira malinga a chitetezo kuzungulira iwo.

Ndime: 2 Mafumu 35: 20-24

Malo a nkhondo: Chigwa cha Megido.

Magulu olimbana: Neko, mfumu ya Igupto, ndi Yosiya, mfumu ya Yuda.

Chifukwa cha nkhondo: Igupto amafuna kuoloka kudzera m'Palestina kukathira nkhondo Nebukadineza, mfumu ya Babulo. Yosiya anawakaniza kudutsa.

Dongosolo la nkhondo:

1. Kanani kunyengedwa: Yosiya anazidzimbaitsa yekha pamene anapita ku nkhondo, poganiza kuti ateteka ku ngozi yonenedwa ndi “mau a Neko kuchokera mkamwa mwa Mulungu” (vs. 22). Chinyengo sichoyenera mu nkhondo yauzimu, chifukwa Satana ndiye wonyenga wamkulu.
2. Mverani Mulungu akalankhula: M'mbuyomu Yosiya anali pa ubale wabwino ndi Mulungu. Ntchito za ubwino wake zikupezeka mu vesi 26. Anadziwa liu la Mulungu, koma apapa sanamvere Mulungu atalankhula.

MAYANKHO A KUYENDERA PERETE

CHAPUTALA 1

1. Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)
2. Gawo la zinthu zathupi ndi gawo la zinthu zauzimu
3. Ufumu wa Mulungu ndi Ufumu wa Satana
4. Satana, ziwanda, dziko ndi thupi
5. Mulungu Atate, Yesu Khristu, Mzimu Woyera ndi angelo
6. Mau oti “mfumu” amanthauza wolamulira wamphamvu wadera kapena anthu.
7. Ufumu ndi dera kapena anthu omwe mfumu imalamulira
8. Nkhondo yauzimu ndi kasanthulidwe ndi kutengapo mbali mu nkhondo yauzimu yosaoneka. Muli kuzindikira mphamvu zolimbana zamdima ndi kuunika, machenjerero a Satana, ndi njira zauzimu zogonjetsera mdani. Nkhondo yauzimu imaposa kungosanthula kufikira kutengapo mbali pogwiritsa ntchito njirazi m'moyo ndi mu utumiki wanu.
9. Chifukwa cha kulimbanaku ndi chakuti Satana amafunabe kukhala wolamulira wamkulu. Akumenya nkhondo mowirikiza kufuna ulamuliro wa moyo, mtima, maganizo ndi mzimu wa munthu.
10. Tikuyenera kudziwa kuti nkhondo zonse za m'moyo, kaya kuthupi, kuuzimu, m'malingiliro, mu mtima, zachuma ngakhale za makhalidwe a anthu ndi chionetsero cha zomwe zikuchitika muuzimu. Ngakhale kuthupi zikhoza kuonekera kudzera mu zochitika za moyo wa tsiku ndi tsiku, koma nkhondo zonsezi zimayambira mdziko lauzimu.

CHAPUTALA 2

1. Cinsinsi ici ncacikuru; koma ndinena ine za Kristu ndi Eklesia. (Luka 5:32)
2. Kulapa ndi “chisankho cha kusintha cha mkati chomwe chimaonekera kunjira kudzera kuchoka ku uchimo kunka kwa Mulungu ndi chilungamo.
3. Onaninso zomwe zakambidwa mu chaputala 2.
4. Munthu akapempha kukhululukidwa kwa machimo amalandira “kutembenuka mtima.” Tikakamba za kutembenuka mtima tikutanthauza “kutembenuka kuchoka ku njira yoipa kunka ku njira yabwino.” Umasiya ufumu wa Satana kulowa Ufumu wa Mulungu.
5. Onaninso zomwe zakambidwa mu chaputala 2.
6. Munthu akalapa machimo napanga chisankho chochoka ku moyo wauchimo ubale wabwino ndi Mulungu umakhazikitsidwa. Ubale umenewu umatchedwa “kulungamitsidwa.”
7. Munthu akalungamitsidwa mwa kulapa ndi kutembenuka mtima, amapulumsidwa ku moyo wa uchimo komanso zilango za uchimo. Izi ndi zimene amanthauza akati

“kupulumutsidwa” ndipo ndi zomwe Baibulo limatanthauza likamanena za kupulumutsidwa.

8. Mnyamata uja atazindikira uchimo wake anapanga chisankho chonka kwa atate wake ndi kukalapa tchimo lake. Izi ndi zimene kulapa kumatanthauza, chisankho cha mkati mwa mtima chomwe chimakhala ndi ntchito. Kenaka ananyamuka naleka moyo wake wakale kunka kwa bambo ake.

CHAPUTALA 3

1. Imvani, Israyeli; Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye mmodzi; (Deuteronomu 6:4)
2. Mulungu Atate, Yesu Khristu, Mzimu Woyera, ndi angelo.
3. Mulungu Atate, Mulungu Mwana, Yesu Khristu; Mulungu Mzimu Woyera.
4. Mulungu Atate ndiye wamkulu wa nkondo wa mphamvu za kuunika zomwe zimalimbana ndi mphamvu zakumdima. Iyi ndi ntchito yake ya padera mu nkondo yauzimu.
5. Ntchito za Yesu Khristu mu nkondo yauzimu ndi: Kupulumutsa munthu ku uchimo: Kudzera mu imfa ya Yesu Khristu tinamasulidwa ku ukapolo wa tchimo womwe Satana anatiyikamo. Ulamuliro pa mphamvu za kumdima: Imfa ya Yesu siinangotimasula ku mphamvu ya uchimo yokha basi, inabweretsa chigonjetso pa mphamvu za kumdima. Chifukwa cha ichi muli ndi ulamuliro pa mdani. Kuonononga ntchito za woipayo: Ichi chinali chimodzi mwa zolinga za Yesu Khristu pobwera pa dziko lapansi ngati munthu. Kupempherera okhulupirira: Yesu ali kumwamba ku dzanja lamanja la mpando wachifumu kupempherera okhulupirira omwe akutenga nawo mbali mu nkondo yauzimu.
6. Mzimu Woyera amatsogolera nkondo ya okhulupirira. Amabvumbulutsa zinthu zauzimu zomwe sizingadziwike mwa umunthu. Iye amalankhula chifuniro ndi Mau a Mulungu kwa ife. Amapemphereranso okhulupirira omwe akuchita nkondo yauzimu. Amapereka mphamvu zauzimu kwa okhulupirira kudzera mu ubatizo wa Mzimu Woyera ndipo amampatsa mpatso ndi chipatso chauzimu.
7. 1 h; 2 d; 3 b; 4 g; 5 l; 6 l; 7 c; 8 a; 9 f; 10 e; 11 j; 12 k.
8. Ambuye wa Makamu

CHAPUTALA 4

1. Mngelo wa Yehova azinga kuwacinjiriza iwo akuopa Iye, Nawalanditsa iwo. (Masalimo 34:7)
2. Kumwamba ndi dziko lapansi
3. Analengedwa ndi Mulungu.
4. Santhulani mautumiki osiyanasiyana za Mzimu Woyera zomwe zakambidwa mu chaputala chino.
5. Santhulani makhalidwe a angelo omwe akambidwa mu chaputala chino.

6. Ahebri 1:14.
7. Zooni. Onani Akolose 2:18 ndi Chibvumbulutso 22:8-9.
8. Si zooni. Onani Agalatiya 1:8.
9. Angelo osankhika
 - Atumiki
 - Akerubi
 - Zamoyo
 - Aserafi
10. Zabwino ndi zoipa
11. Akolose 1:16

CHAPUTALA 5

1. Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire: (1 Petro 5:8)
2. Satana poyamba analengedwa ndi Mulungu ngati mngelo.
3. Poyambapo amatchedwa Lucifala, mkerubi wodzodzedwa.
4. Satana anachotsedwa kumwamba chifukwa ma kudzitama komwe kunaonekera kudzera m' mau ake asanu akuti, "Ndidza."
5. Onani zotsatira zomwe ziri mu Chaputala 5.
6. Satana amagwira ntchito kumwamba komanso pano padziko.
7. Machitachita a Satana nthawi zonse amakhala olimbana ndi Mulungu, Mau ake, dongosolo lake, anthu ake, kupembedza kwao, kuyenda kwao, ndi ntchito zawo.
8. Werengani mndandanda womwe uli mu Chaputala 5.

CHAPUTALA 6:

1. Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m' masiku otsiriza ena adzataya cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunziro a ziwanda, (1 Timoteyo 4:1)
2. Mulungu ndiye anawalenga.
3. Dera lawo logwirira ntchito ndi dziko lapansi.
4. Ngati Satana, ntchito zawo zimakhala zolimbana ndi Mulungu, dongosolo lake, ndi anthu ake.
5. Onani mndandanda wa makhalidwe womwe uli mu Chaputala 6.
6. Onani kusanthula komwe kuli mu Chaputala 6.
7. Poyamba anali angelo kumwamba.
8. Anatenga nawo gawo nkuukira kwa Satana ndipo zinachotsedwa kumwamba. Sanakhalenso angelo abwino koma ziwanda.
9. Onani kusanthulidwa kwa nkhani iyi mu Chaputala 6.

CHAPUTALA 7.

1. Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko apansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, cikondi ca Atate Isiciri mwa iye. Pakuti ciri conse ca m'dziko lapansi, cilakolakoca thupi ndi cilakolako ca maso, matamandidwe a moyo, sizicokera kwa Atate, koma ku dziko lapansi. (1 Yohane 2:15-16)
2. Mau oti “thupi” omwe akugwiritsidwa ntchito mu chaputala chino akutanthauza chikhalidwe cha uchimo cha mwa munthu aliyense chomwe chimatsutsana ndi ndi dongosolo la Mulungu.
3. Mau oti “dziko” omwe agwiritsidwa ntchito mu chaputala chino akutanthauza dongosolo la dziko lapansi lomwe limatsutsana ndi chifuniro cha Mulungu.
4. Satana.
5. Yerekezani zomwe mwapeza ndi zomwe ziri mu Chaputala 7.
6. Tchimo.
7. Dziko limadana ndi okhulupirira
8. Chilakolako choipa ndi chikhumbokhumbo chachikuru chomwe munthu amamva mkati mwake, chomkokera ku uchimo. Kulakalaka zinthu zoipa zompangitsa munthu kuchimwa kumatchedwa, “chilakolako cha thupi.”
9. Satana amagwiritsa ntchito zomwe zamzungulira munthu kumkopa kudzera mu kumva, kukhudza, kulawa, kuona, ndi kununkhiza kuti amuchimwitse.
10. Chilakolako chimabala yesero, yesero limabala tchimo, ndipo tchimo limabala imfa.
11. Agalatiya 5:19-21

CHAPUTALA 8.

1. Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire: ameneyo mumkanize okhazikika m'cikhulupiriro, podziwa kuti zowawa zomwezo zirimkukwaniridwa pa abale anu ali m'dziko.(1 Petro 5:8-9)
2. Werengani zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 8.
3. Werengani zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 8.
4. Werengani zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 8.
5. Werengani zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 8.

CHAPUTALA 9

1. iye wocita cimo ali wocokera mwa mdierekezi, cifukwa mdierekezi amacimwa kuyambira paciyambi. Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge nchito za mdierekezi, (1 Yohane 3:8)
2. Werengani zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 9.
3. Kuti akaononge ntchito za mdierekezi.

4. Mau a Mulungu, mphamvu ndi ulamuliro, pemphero, kusala kudya, mfungulo za mu Ufumu wa Mulungu, ndi dzina la Yesu.

CHAPUTALA 10

1. Ndipo musampatse mpata mdierekezi.
2. Nkhondo yodziteteza ndi nkhondo yomenyedwa pofuna kuteteza dera ndi katundu. Imadikira mdani abwere ndikupalamula, kenako m'masonkhanitsa zida zanu ndikuyambapo kuteteza dera. Mtundu wa nkhondo iyi sulowa m'dera la mdani. Umateteza dera lomwe lalandidwa kale.
3. Nkhondo yopalamula ndi nkhondo ya makani koposa. Siidikira kuti mdani adzapalamule ayi. Ndi pamene mukathira adani anu nkhondo. M'madziwa mdani, ndi njira zake kenaka mumthira nkhondo muuzimu.
4. Mu nkhondo zonsezi, munthu wokhulupirira akuyenera kutengapo gawo lalikuru.
5. Werengani zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 10.
6. Werengani zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 10.

CHAPUTALA 11

1. Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi. (Aefeso 6:11).
2. Werengani zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 10.
3. Aefeso 6:13-17
4. Onani zolembedwa pa mutu wa zida zauzimu za nkhondo mu Chaputala 11.

CHAPUTALA 12

1. Yehova watsegula pa nyumba ya zida zace, ndipo waturutsa zida za mkwiyo wace; pakuti Ambuye Yehova wa makamu, ali ndi nchito m'dziko la Akasidi. (Yeremiya 50:25a)
2. Yerekazani zolembedwa mwachidule zanu ndi zolembedwa mu pa mutu uwu mu Chaputala 12.

CHAPUTALA 13.

1. Lamulo ili ndipereka kwa iwe, mwana wanga Timoteo, kuti, emonga mwa zonenera zidakutsogolera iwe kale, ulimbane nayo nkhondo yabwino; (Timoteyo 1:18)
2. Mfundo za kuthupi zikugwiritsidwa ntchito pofotokozera zomwe zikuchitika muuzimu. Timamvetsa bwino zomwe zikuchitika mu dziko la kuthupi. Zinthu zakuuzimu zikafaniziridwa ndi za kuthupi, timazimvetsa bwino popeza zakuthupi ndi zoti timazidziwa kale. Mulungu akuyerekeza zakuuzimu ndi zakuthupi polankhula za nkhondo yauzimu, popeza zimafanana.
3. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi zomwe zalembedwa mu Chaputala 13.

CHAPUTALA 14.

1. podziwa ici, kuti umunthu wathu wakale unapacikidwa pamodzi ndi iye, kuti thupilo la ucimo likaonongedwe, kuti ife tisakhalenso akapolo a ucimo; pakuti iye amene anafa anamasulidwa kuucimo. (Aroma 6:6-7)
2. Machenjerero ndi ukadaulo wokonza ndi kukwaniritsa dongosolo la nkhondo. Ndi dongosolo lotsogera ku chipambano.
3. Mau akuti “kutsutsa” akutanthauza kuchita mosemphana, kuletsa, kapena kufooketsa. Njira yotsutsira ndi dongosolo lokonzedwa mwa ukadaulo lokanizira kapena kugonjetsa machenjerero a Satana ndi ziwembu zake.
4. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 14.
5. Yerekezani zolembe mwachidule zani ndi zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 14.

CHAPUTALA 15

1. Pakuti pakuyendayenda m'thupi, siticita nkhondo monga mwa thupi, (pakuti zida za nkhondo yathu siziri za thupi, koma zamphamvu mwa Mulungu zakupasula malinga); ndi kugwetsa matsutsano, ndi cokwezeka conse cimene cidzikweza pokana dddziwitso ca Mulungu, ndi kugonjetsa ganizo lonse ku kumvera kwa Kristu; (2 Akorinto 10:3-5)
2. M'malingiliro.
3. Ndi mivi yoyaka moto ya mdierekezi. Mdani amakhala akuponya “mivi yoyaka moto” pa ife muuzimu. Mivi yambiri amailunjikitsa ku malingiliro.
4. Yerekezani zolembe mwachidule zani ndi zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 15.
5. Yerekezani zolembe mwachidule zani ndi zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 15

CHAPUTALA 16.

1. koma lilime palibe munthu akhoza kulizoloweretsa; liri coipa cotakataka, lodzala ndi ululu wakupha. (Yakobo 3:8)
2. Lilime.
3. Yerekezani zolembe mwachidule zani ndi zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 16.
4. Yerekezani zolembe mwachidule zani ndi zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 16.

CHAPUTALA 17.

1. Koma ndinawabwezera mau, ndi kunena nao, Mulungu Wam'mwamba, Iye ndiye adzatilemeza; cifukwa cace ife akapolo ace tidzanyamuka ndi kumanga; koma inu mulibe gawo, kapena ulumuliro, kapena cikumbukilo, m'Yerusalemu. (Nehemiya 2:20).
2. Yerekezani zolembe mwachidule zani ndi zolembedwa pa mutu uwu mu Chaputala 17.
Malinga anu auzimu omwe Satana amafuna atawaononga ndi:
 - Malinga a chipulumutso, zipata za matamando
 - Ntchito ya mtanda m'moyo wanu

- Umboni wa Chikristu
 - Munthu wakale kusinthika kukhala watsopano
 - Kusautsidwa ndi kuyesedwa
 - Kuthana ndi ntchito za thupi
 - Ntchito ya Mzimu Woyera
 - Mau a Mulungu
 - Nkhondo yauzimu
 - Chiyembekezo cha kubweranso kwa Yesu
 - Kudziyesa wekha
3. Tchimo
 4. Yerekeza mndandanda wanu ndi zomwe zaperekedwa mu Chaputala 17.
 5. Yerekezani mndandanda wanu ndi njira zomwe ziri mu Chaputala 17.

CHAPUTALA 18.

1. Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10).
2. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi machenjerero a Satana pa thupi la munthu omwe aperekedwa mu Chaputala 18.
3. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi njira zotsutsira machenjerero ku chigonjetso cha thupi lanu molingana ndi zomwe ziri mu Chaputala 18
4. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi machenjerero a Satana pa makhalidwe a munthu omwe aperekedwa mu Chaputala 18.
5. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi njira zotsutsira machenjerero ku chigonjetso cha nkhondo ya makhalidwe a anthu molingana ndi zomwe ziri mu Chaputala 18
6. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi machenjerero a Satana pa banja omwe aperekedwa mu Chaputala 18.
7. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi njira zotsutsira machenjerero ku chigonjetso cha pa banja molingana ndi zomwe ziri mu Chaputala 18
8. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi machenjerero a Satana pa chuma ndi ndalama omwe aperekedwa mu Chaputala 18.
9. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi njira zotsutsira machenjerero ku chigonjetso cha pa chuma ndi ndalama molingana ndi zomwe ziri mu Chaputala 18.

CHAPUTALA 19

1. Ndipo anathamanga anyamata, nauza Mose, nati, Elidadi ndi Medadi alikunenera m'cigono. (Numeri 11:27).
2. Kusamutsa kumatanthauza kupereka kuchokera kwa munthu wina kupita kwa winanso. Mau akuti “mzimu” omwe agwiritsidwa ntchito mu phunziro lino akutanthauza chikhalidwe, maonedwe a zinthu, kapena cholinga pa chochitika chirichonse. Munthu

atha kumalamuliridwa ndi Mzimu wa Mulungu kapena mzimu woipa ndi kusamutsa mzimuwo kwa ena mwina ngati munthu payekha kapena ngati gulu.

3. Nkhani ya Mose ndi akulu 70 mu Numeri 11:16-17.
4. Nkhani ya azondi khumi mu Numeri 13.
5. Letsani mzimu wanu.
Yang'anirani lilime lanu.
Yang'anira zokonda zanu.
Sankhani abwenzi anu mosamala.
Yang'anira zomvaimva mthupi lanu.
Khalani wosamala "posanjika manja."

CHAPUTALA 20.

1. Ndipo kulibe kudabwa; pakuti Satana yemwe adzionetsa ngati mngelo wa kuunika. Cifukwa cace sikuli kanthu kwakukuru ngatinso atumiki ace adzionetsa monga atumiki a cilungamo; amene cimariziro cao cidzakhala monga nchito zao. (2 Akorinto 11:14-15).
2. Amagwiritsidwa ntchito pa kupembedza.
3. Paulo akamalankhula za "zoipa zauzimu m'malo okwera" akulankhula za mizimu yoipa yomwe yalowa m'madongosolo a zipembezo za dziko lapansi. Mizimuyi yalowa ngakhale m'mabwalo a olungama.
4. Yerekezani zolemba mwachidule zanu ndi zomwe zalembedwa mu Chaputala 20.
5. Yerekezani yankho lanu ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 20.

CHAPUTALA 21.

1. Za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Machitidwe 10:38).
2. Mizimu yonyenga, mizimu yamatenda, ndi mizimu yoipa.
3. Mphatso ya kuzindikira mizimu imampatsa wokhulupirira kuthekera kotha kudziwa mzimu womwe ukugwira ntchito mwa munthu komanso kudziwa mwamsanga ngati munthu ali ndi mzimu woipa ndipo kuti ndi wantundu wanji. Mphatsoyi imaletsa chinyengo cha mizimu yokopa ndi ya bodza. Munthu amene ali ndi mphatsoyi amazindikira machenjerero ndi zolinga zoipa za mphamvu ya ziwanda.
4. Kugwidwa ndi ziwanda ndiko kukhala ndi mzimu kapena mizimu yoipa (ziwanda) m'thupi la munthu ndikulamulira moyo wake kwatunthu.
5. Yerekezani mndandanda wanu ndi mndandanda womwe waperekedwa mu Chaputala 21.
6. Kudzadzidwa ndi ziwanda kumatanthauza kukhala ndi chidwi chopitirira muyezo ndi ziwanda, Satana ndi zamatsenga.
7. Yerekezani mndandanda wanu ndi mndandanda wa mu Chaputala 21.

8. Kuponderezedwa ndi ziwanda ndiye kuti mphamvu ya ziwanda imakupanikiza, kutsutsana nawe kapena kukumanga koma ziri kunjira kwako.
9. Yerekezani mndandanda wanu ndi mndandanda womwe waperekedwa mu Chaputala 21
10. Yerekeani zolembe mwachidule zanu ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 21.

CHAPUTALA 22

1. Umve zowawa pamodzi nane ngati msilikari wabwino wa Yesu Khristu (2 Timoteyo 2:3).
2. Tchimo ndi Satana.
3. Onaninso njira zisanu zomwe mavuto amabwelera m'moyo wa munthu wokhulupirira zomwe ziri mu Chaputala 22.
4. Onaninso phindu lomwe wokhulupirira amalipeza akalowa mu zovuta molingana ndi chaputala chino.
5. Onaninso za kaonedwe kabwino ka mavuto komwe kakambidwa mu Chaputala 22.
6. a. Sizoon; b. Sizoon; c. Sizoon; d. Zoon.

CHAPUTALA 23.

1. Ndalimbana nako kulimbana kwabwino. Ndamaliza njira yanga. Ndasunga chikhulupiriro (2 Timoteo 4:7).
2. Davide, Yoswa, Eliya ndi Paulo.
3. Zindikira kulephera kwako.
Lapa.
Toleranso mphamvu zako zauzimu.
Bweleranso ku nkondo.
4. Aroma 8:1.
5. 2 Timoteyo 2:26.
6. Kutu sitingathe kudzialira tokha pa nkondo yauzimu. Kudalira kwathu kuli mwa Mulungu.

CHAPUTALA 24.

1. Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyedwa m'nyanja ya mota ndi sulfure, kumeneko kulinso ciomboco ndi mneneri wonyengayo; ndipo adzazunzidwa usana ndi usiku ku nthawi za nthawi. (Chibvumbulutso 20:10).
2. Yerekezani zolembe mwachidule zanu ndi zomwe ziri mu Chaputala 24.
3. Nkhondo yomaliza idzachitika zitatha zakha chikwi za ulamuliro wa Yesu pamene Satana adzamasulidwe kwa kamphindi. Moto wochokera kumwamba udzatsika ndi kuonononga mphamvu za woipa. Satana ndi mphamvu zakumdima adzapita ku malo awo omaliza.

4. Adzaponyedwa mu yoyaka moto wa sufure ndi kuzunzika kwa muyaya.